# TESTAMENTE WATSOPANO

WA

# MWINI WATU NDI MPULUMUTSI

# YESU KRISTU.

---

MAU A TSHINYANJA.

---

EDINBURGH

PRINTED FOR THE NATIONAL BIBLE SOCIETY

OF SCOTLAND.

1900.

Chinyanja New Testament.]

## MAINA NDI KUNDANDALIKA

ZA

# MABUKU ONSE A TESTAMENTE WATSOPANO.


| | | Peje |
|---|---|---|
| Mateyu | Mat. | 1 |
| Marko | Mar. | 55 |
| Luka | Lu. | 89 |
| Yohane | Yoh. | 148 |
| Ntshito za Apostile | Ntsh. | 190 |
| Epistola la Paulos kwa Aroma | Rom. | 248 |
| Epistola latshimodzi la Paulos kwa Akorinte | 1 Kor. | 272 |
| Epistola latshiwiri la Paulos kwa Akorinte | 2 Kor. | 294 |
| Epistola la Paulos kwa Agalatiya | Gal. | 310 |
| Epistola la Paulos kwa Afeso | Fes. | 317 |
| Epistola la Paulos kwa Afilipi | Fil. | 325 |
| Epistola la Paulos kwa Akolose | Kol. | 331 |
| Epistola latshimodzi la Paulos kwa Atesalonika | 1 Tes. | 336 |
| Epistola latshiwiri la Paulos kwa Atesalonika | 2 Tes. | 341 |
| Epistola latshimodzi la Paulos kwa Timote | 1 Tim. | 344 |
| Epistola latshiwiri la Paulos kwa Timote | 2 Tim. | 350 |
| Epistola la Paulos kwa Tito | Ti. | 354 |
| Epistola la Paulos kwa Filemon | File. | 357 |
| Epistola kwa Ahebere | Heb. | 358 |
| Epistola la Yakobi | Yak. | 377 |
| Epistola latshimodzi la Petros | 1 Pet. | 383 |
| Epistola latshiwiri la Petros | 2 Pet. | 389 |
| Epistola latshimodzi la Yohane | 1 Yoh. | 393 |
| Epistola latshiwiri la Yohane | 2 Yoh. | 399 |
| Epistola latshitatu la Yohane | 3 Yoh. | 400 |
| Epistola la Yuda | Yu. | 401 |
| Kusonyeza kwa Yohane | Kus. | 403 |

# IVANGELI WA MATEYU.

BUKU la fuko la Yesu Kristu, mwana wa Davide, 1
mwana wa Abraham.

Abraham wabala Yisake; ndimo Yisake wabala Yakobi; 2
ndimo Yakobi wabala Yuda ndi abali atshi; ndimo Peretse 3
ndi Zera, Yuda wabala ndi Tamare; ndimo Peretse wabala
Hetseron; ndimo Hetseron wabala Aram; ndimo Aram 4
wabala Haminadabi; ndimo Haminadabi wabala Nashon;
ndimo Nashon wabala Salimon; ndimo Salimon wabala 5
Bowaze ndi Rahabi; ndimo Bowaze wabala Hobede ndi
Rute; ndimo Hobede wabala Yishayi; ndimo Yishayi 6
wabala Davide fumu yotshuka.

Ndimo Davide wabala Solomon ndi *iemwe anali nkazi*
wa Huriya; ndimo Solomon wabala Rehabam; ndimo 7
Rehabam wabala Abiya; ndimo Abiya wabala Asa; ndimo 8
Asa wabala Yoshafati; ndimo Yoshafati wabala Yoram;
ndimo Yoram wabala Huziya; ndimo Huziya wabala Yotam; 9
ndimo Yotam wabala Ahazi; ndimo Ahazi wabala Hezekiya;
ndimo Hezekiya wabala Manase; ndimo Manase wabala 10
Amon; ndimo Amon wabala Yoshiya; ndimo Yoshiya 11
wabala Yekoniya ndi abali atshi, pa ntawi ya kutengedwa
ku Babilon.

Ndimo pambuiu kutengedwa ku Babilon, Yekoniya wabala 12
Shelatiyeli; ndimo Shelatiyeli wabala Zerubabeli; ndimo
Zerubabeli wabala Abihude; ndimo Abihude wabala 13
Eliyakim; ndimo Eliyakim wabala Hazore; ndimo Hazore
wabala Tsadoki; ndimo Tsadoki wabala Akim; ndimo 14
Akim wabala Eliyudi; ndimo Eliyudi wabala Elazari; ndimo 15
Elazari wabala Matan; ndimo Matan wabala Yakobi;
ndimo Yakobi wabala Yosefe mamuna wa Mariya, kwa emwe 16
wabadwa Yesu, emwe atshedwa Kristu.

Monga mafuko onse kwa Abraham ndi Davide ali mafuko 17
kumi ndi anai; ndimo kwa Davide ndi kutengedwa kwa
Babilon mafuko kumi ndi anai; ndimo kwa kutengedwa
kwa Babilon ndi Kristu mafuko kumi ndi anai.

18 Ndimo kubadwa kwa Yesu Kristu kunali tshointshi:
Ntawi amai atshi Mariya anawindikidwa ndi Yosefe, patsogolo
anakomana anapezedwa ali mimba ya Nzimu Woyera.
19 Ndimo Yosefe mamuna watshi, anali wodeka, ndimo sana
20 funa ku nyazitsa ie, naganiza kumtshotsa kutseri. Koma
ntawi anaganiza ndi zintu zimenezi, ona, njelo wa Mwini
nadzisonya kwa ie m' kulota, kuti, Yosefe, mwana wa
Davide, usaopa ku tenga kwa iwe Mariya nkazi wako : kuti
21 emwe wabvuukidwa mwa ie ali wa Nzimu Woyera. Ndimo
adzabala mwana; ndimo udzatsha dzina latshi Yesu; kuti
ali ie emwe adzapulumutsa antu atshi kwa zakwaipa zao.
22 Ndimo zonse zimenezi zinakala, monga kuti anangodzazidwa
omwe ananenedwa ndi Mwini mwa mprofeti, kuti,
23 Ona, tshiweta tshidzakala ndi mwana, ndimo adzabala
mwana wamamuna,
Ndimo adzatsha dzina latshi Manuweli;
24 lomwe liri, lasandukidwa, Mulungu ndi ife. Ndimo Yosefe
nauka kwa tulo tatshi, natshita monga njelo wa Mwini
25 anamuza, natenga kwa ie nkazi watshi; ndimo sanadziwa ie
kwa ntawi nabala mwana wamamuna: ndimo natsha dzina
latshi Yesu.

2 Ndimo ntawi Yesu anabadwa m' Betelehem wa Yudeya
m' masiku a Herode fumu yotshuka, ona, nadzera amuna
2 otshenjera ku bvuma ku Yerusalem, kuti, Alikuti ie emwe
abadwa Fumu Yotshuka ya Ayuda? kuti tinaona nyenyezi
3 yatshi m' bvuma, ndimo tinadza ku pembedza ie. Ndimo
ntawi Herode fumu yotshuka anatshimva, nasautswa, ndi
Yerusalem wonse ndi ie. Ndimo kusong'kanitsa adzukuru
4 akuru onse ndi akulembera a antu, watuzula kwa awo pomwe
5 Kristu akabadwa. Ndimo nanena nai', M' Betelehem wa
Yudeya: kuti tshointshi alembedwa ndi mprofeti,
6 Nawe Betelehem, dziko la Yuda,
Usali woung'ono wopambana mwa otshuka a Yuda:
Kuti kwa iwe adzaturuka woweruza,
Emwe adzabusa antu anga Asirayeli.
7 Ndimo Herode anaitana kutseri antu otshenjera, nafunsira
8 kosamala ndi awo ntawi bwanje nyenyezi inasonyeza. Natumiza
awo ku Betelehem, nati, Endani, funani kosamala
ndi kamwana; ndimo ntawi mudza*m*peza, bwezani mau kwa
ine, monga kuti ine enso dingodza ndingopembedza ie.
9 Ndimo awa, anamva fumu yotshuka, namuka; ndimo ona,
nyenyezi, yomwe naiwona m' bvuma, inang'ka patsogolo

pa awo kwa ntawi inafika ndimo inaima pamwamba pomwe
kamwana kanali. Ndimo ntawi naona nyenyezi, nasekera 10
ndi tshimwemwe tshatshikuru tshambiri. Ndimo naloa 11
m' nyumba, naona kamwana ndi Mariya amai atshi; na-
gwada napembedza ie; ndimo kutsegula zolemera zao,
napatsa kwa ie zolere, golide ndi nardo ndi more. Ndimo 12
analangizidwa *ndi Mulungu* m' kulota kuti sakabwera kwa
Herode, nang'ka ku dziko lao ndi njira ina.

Ndimo ntawi namuka, ona, njelo wa Mwini adzisonya m' 13
kulota ku Yosefe, kuti, Dzuka, tenga kamwana ndi amai
atshi, nutawira ku Yiputa, nukala uko kwa ntawi dinena
ndi iwe: kuti Herode adzafuna kamwana kukamwaza.
Ndimo nauka natenga kamwana ndi amai atshi usiku, 14
nang'ka ku Yiputa; nakala uko kwa ntawi ya imfa ya 15
Herode: kuti anangodzazidwa omwe ananenedwa ndi Mwini
mwa mprofeti, kuti, Kwa Yiputa dinaitana mwana wanga.
Ndimo Herode, ntawi naona kuti anapusitsidwa ndi antu 16
otshenjera, nakwiira kwambiri, natumiza, napa tiana tati-
muna tonse tomwe tinali m' Betelehem, ndi m' miraga yonse
ya iwo, kwa dzaka dziwiri ndi ito ta dzaka dzosafika, monga
ntawi yomwe anafunsira kosamala ndi amuna otshenjera.
Ndimo anadzazidwa omwe ananenedwa ndi Yeremiya 17
mprofeti, kuti,

Liu linamvedwa m' Rama, 18
Kulira misozi ndi maliro ambiri,
Raheli kulirira ana atshi;
Ndimo sanafuna ku sangalatsidwa, tshifuka kuti osali.

Koma ntawi Herode anafa, ona, njelo wa Mwini adzisonya 19
m' kulota ku Yosefe m' Yiputa, kuti, Dzuka, tenga kamwana 20
ndi amai atshi, numuka ku dziko la Sirayeli: kuti anafa
omwe nafuna moyo wa kamwana. Nauka natenga kamwana 21
ndi amai atshi, nadza m' dziko la Sirayeli. Koma ntawi 22
anamva kuti Arkelawo analikuweruza m' Yudeya m' malo
a atatu atshi Herode, naopa ku ng'ka uko; koma kulangi-
zidwa *ndi Mulungu* m' kulota, nalambalala m' miraga ya
Galileya, nadza nakala muzinda watshedwa Nazarete: 23
monga kuti anangodzazidwa omwe ananenedwa ndi aprofeti,
kuti akatshedwa Mnazarete.

Ndimo m' masiku adya adza Yohane Mbapatizi, kuuza 3
m' tshipululu tsha Yudeya, kuti, Tembenukani; kuti dziko 2
la kumwamba liri pafupi. Kuti amene ali ie emwe anane- 3
nedwa ndi mprofeti Yesaya, kuti,

Liu la modzi kupfula m' tshipululu,
Fotokozani njira ya Mwini,
Pangani njira zatshi zolungama.
4 Ndimo Yohane ie eka anali ndi nsaru zatshi za ubwea wa
gamila, ndi lamba la tshikopa mtshunu mwatshi; ndi kudia
5 kwatshi kunali madzombe ndi utshi wa mutengo. Ndimo
naturuka kwa ie Yerusalem, ndi Yudeya lonse, ndi dziko
6 lonse mbali mwa Yordan; ndimo anabapatizidwa ndi ie m'
7 ntsinje Yordan, kubvumbula zakwaipa zao. Koma ntawi
naona ambiri a Afarisi ndi a Asadusi adza ku mbapatisma
latshi, nanena nao, Fuko la zinjoka, ndani walangiza inu
8 ku tawa kwa kukwiira kulinkudza? Ndimo balani dzobala
9 dzabwino kwa kutembenuka: ndimo musaganiza ku ti mwa
inu noka, Tiri ndi Abraham, ali atatu atu: kuti dinena ndi
inu, kuti Mulungu adziwa kwa miala imene ku kulitsa ana
10 kwa Abraham. Ndimo inde tsopano nkwangwa iikidwa pa
ntsitsi wa mitengo: ndimo mitengo yonse yomwe yosabala
11 dzobala dzabwino itemedwa, niponyedwa pa moto. Dibapa-
tiza inu nditu ndi madzi kwa kutembenuka: koma iemwe
adza pambuiu pa ine ali wampamvu wopambana ine,
dzikwakwata dza emwe sindiri woenera ku nyamula: ie
12 adzabapatiza inu ndi Nzimu Woyera ndi moto: litshero la
emwe liri m' dzanja latshi, ndimo adzapetetsa bwino mbua
yatshi; nadzasong'ka trigu watshi m' nkokwe, koma
adzaotsha mungu ndi moto wosazima.
13 Ndimo Yesu adzera kwa Galileya ku Yordan kwa Yohane,
14 ku bapatizidwa ndi ie. Koma Yohane nafuna ku dzudzula
ie, kuti, Diri ndi kufunidwa ku bapatizidwa ndi iwe, ndimo
15 udza kwa ine kodi? Koma Yesu kuiang'ka nanena nai',
Leka iko tsopano: kuti tshointshi kuli kwabwino kwa ife
16 ku dzaza kudeka konse. Ndimo abvomera ie. Ndimo
Yesu, ntawi anabapatizidwa, naturuka nsanga ku madzi:
ndimo ona, miamba inatsegulidwa kwa ie, naona Nzimu wa
17 Mulungu nutsika monga njiwa, nukaka pa ie; ndimo ona,
liu kwa miamba, kuti, Amene ali Mwana wanga wondikonda,
ndi emwe disekera bwino.

4 Ndimo Yesu natsogozwa ndi Nzimu m' tshipululu ku
2 yesedwa ndi diabolos. Ndimo ntawi analibe kudia madzua
makumi anai, ndi masiku makumi anai, pambuiu, anamva
3 njala. Ndimo woyesa nadza nanena nai', Ngati uli Mwana
wa Mulungu, uza kuti miala imene ipangike mikate. Koma
naiang'ka nati, Alembedwa, Muntu wosadzakala ndi moyo

udi mikate yoka, koma ndi mau onse omwe aturuka m'
nkamwa mwa Mulungu. Ndimo diabolos amtenga ku 5
mzinda woyera; naika ie pa tshimbudzi tsha tempile, ndimo 6
anena nai', Ngati uli Mwana wa Mulungu, udziponye pansi:
kuti alembedwa,

Adzauza anjelo atshi ndi iwe:
Ndi m' manja mao adzatukula iwe,
Kani kapena udzagunda pazi lako ndi mwala.

Yesu nanena nai', Alembedwa anso, Usayesa Mwini
Mulungu wako. Onso, diabolos atenga ie ku piri lali- 8
tali kwambiri, nasonyeza ie maiko onse a dziko, ndi
kupambana kwa awo; ndimo nanena nai', Zintu zonse 9
zimenezi didzakupatsa, ngati udzagwada nudzapembe-
dza ine. Ndimo Yesu anena nai', Tshoka, Satana: kuti 10
alembedwa, Udzapembedza Mwini Mulungu wako, ndi ie
eka udzaimirira. Ndimo diabolos amsia; ndimo ona, anjelo 11
nadza naimirira kwa ie.

Ndimo ntawi anamva kuti Yohane anaperekedwa, namuka 12
ku Galileya; ndimo kusia Nazarete, nafika nakala m' 13
Kapernahum, womwe uli mbali mwa nyanja, m' maliri a
Zebulon ndi Nafetali: monga kuti anangodzazidwa omwe 14
ananenedwa ndi Yesaya mprofeti, kuti,

Dziko la Zebulon ndi dziko la Nafetali, 15
Pa njira ya nyanja, patsidia la Yordan,
Galileya la Mitundu,
Antu omwe nakala mudima 16
Naona kuunika kwakukuru,
Ndi kwa awo omwe anakala m' dziko, ndi mutunzi
za imfa,
Kwa awo kuunika kunafika.

Kwa ntawi imene Yesu naamba ku uza, ndi ku nena, 17
Tembenukani; kuti dziko la kumwamba liri pafupi.

Ndimo kuendaenda mbali mwa nyanja ya Galileya, naona 18
abali awiri, Simon emwe atshedwa Petros, ndi Andreya
mpwatshi, kuponya koka m' nyanja; kuti anali apodzo.
Ndimo anena nao, Tsatani ine, ndidzapanga inu apodzo a 19
antu. Ndimo tsopano lino nasia maukonde, natsata ie. 20
Ndimo kuenda komwe naona abali ena awiri, Yakobi *mwana* 21
wa Zebediya, ndi Yohane mpwatshi, m' tshombo ndi
Zebediya atatu ao, analikusoka maukonde ao; naitana
awo. Ndimo tsopano lino nasia tshombo ndi atatu ao, 22
natsata ie.

23 Ndimo Yesu naendaenda m' Galileya lonse, kupunzitsa
m' masinagoge ao, ndimo kuuza ivangeli wa dziko,
ndi kutshiritsa mitundu yonse ya kudwala ndi mitundu
24 yonse ya ntenda mwa antu. Ndimo mbiri ya ie
inaendaenda mwa Siriya lonse: natenga kwa ie onse
omwe anali odwala, ogwidwa ndi ntenda zina ndi
maululu, apotsheredwa ndi ademon, ndi atshizumbazumba,
25 ndi onjenjemera; natshiritsa awa. Namtsata ie antu ambiri
kwa Galileya ndi Dekapolis ndi Yerusalem ndi Yudeya
ndi *kwa* patsidia la Yordan.

5 Ndimo kuona antu ambiri, nakwera pa piri: ndimo ntawi
2 nakala pansi, akupunzira atshi nafika kwa ie: natsegula
nkamwa mwatshi napunzitsa awa, kuti,
3 Odala ali osauka ndi mizimu: kuti lao liri dziko la
kumwamba.
4 Odala ali omwe amva tshisoni: kuti adzasangalatsidwa.
5 Odala ali oanja: kuti adzaloezedwa dziko.
6 Odala ali awo omwe amva njala ndi ludzu kwa kudeka:
kuti adzadzazidwa.
7 Odala ali ansisi: kuti adzalandira nsisi.
8 Odala ali oyera muntima: kuti adzaona Mulungu.
9 Odala ali oletsetsa: kuti adzatshedwa ana a Mulungu.
10 Odala ali awo omwe anazunzidwa kwa kudeka: kuti lao
11 liri dziko la kumwamba. Odala muli inu ntawi *antu*
adzasinjirira inu, nadzazunzitsa inu, nadzanena mitundu
12 yonse ya mpulupulu pa inu konama, kwa ine. Kondwerani,
ndi sekerani kwambiri: kuti lalikuru liri sekeretso lanu m'
mwamba: kuti tshointshi anazunzitsa aprofeti omwe anali
patsogolo pa inu.
13 Muli ntshere wa dziko: koma ngati ntshere unataiika
nyongo yatshi, ndi tshiani udzakometsedwa? kwa ntawi
imene uli wabwino kwa tshabe, koma ku turutsidwa ndi ku
14 pondedwa ndi mapazi a antu. Muli kuunika kwa dziko.
15 Mzinda uikidwa pa piri wosadziwa ku bisidwa. Kapena
*antu* osakoleza nyali naiika pansi pa ntanga, koma pa
tshogwirira nyali; ndimo iwala kwa onse omwe ali m'
16 nyumba. Inde tshointsho lekani kuunika kwanu kwiyera
patsogolo pa antu, kuti aone ntshito zanu zabwino, napa-
mbanitse Atatu anu emwe ali m' mwamba.
17 Musaganiza kuti dinadza ku mwaza mau kapena aprofeti:
18 dinadza si ku mwaza, koma ku dzaza. Kuti dinena ndi
inu nditu, Kwa ntawi kumwamba ndi dziko zipita, iota

imodzi kapena kakang'ono kamodzi sizidzapita nditu kwa
mau, kwa ntawi zintu zonse zidzatedwa. Ndimo emwe 19
adzaswa modzi wa mau amene ang'ono, ndimo adzapunzitsa
antu tshointshi, adzatshedwa wang'ono wopambana m' dziko
la kumwamba: koma emwe adzatshita nadzapunzitsa awo,
adzatshedwa wang'kuru m' dziko la kumwamba. Kuti 20
dinena ndi inu, kuti, kani kudeka kwanu kudzapambana
*kudeka* kwa akulembera ndi Afarisi, musadzaloa nditu
m' dziko la kumwamba.

Munamva kuti kunanenedwa ndi awo akali, Usapa; ndi 21
emwe adzapa adzasetsherezwa kwa kuweruza: koma dinena 22
ndi inu, kuti emwe akwia ndi mbali watshi adzasetsherezwa
kwa kuweruza; ndi emwe adzanena ndi mbali watshi, Raka,
adzasetsherezwa kwa gulu la ankoswe; ndi emwe adzanena,
Wopusa iwe, adzasetsherezwa kwa geena wa moto. Ndimo 23
ngati ulikutsira mtulo wako pa katshisi, ndimo apo ukumbu-
kila kuti mbali wako ali ndi kantu pa iwe, sia apo mtulo 24
wako patsogolo pa katshisi, numuka, patsogolo anjanitswa
ndi mbali wako, ndimo pomwe udza nutsira mtulo wako.
Anjanitsa ndi liwongo lako nsanga, ntawi uli pa njira ndi 25
ilo; kani kapena liwongo likapereka iwe kwa woweruza,
ndi woweruza akapereka iwe kwa kazembe, ndimo uikidwa
m' nyumba ya ndima. Dinena ndi iwe nditu, Sudzaturu- 26
kiratu umo, kwa ntawi unalipidwa fardin lakutungo.

Munamva kuti kunanenedwa, Usatshita tshigololo: koma 27
dinena ndi inu, kuti emwe aang'ana nkazi ku funa ie 28
anatshita tshigololo ndi ie tsopano muntima mwatshi.
Ndimo ngati diso lako lamanja likutshimwitsa, tshotsa, 29
nulitaia iwe: kuti kuli kwakupindulidwa kwa iwe kuti
tshimodzi tsha dziwalo dzako tshikamwazika, ndimo si tupi
lako lonse likataiikidwa m' geena. Ndimo ngati dzanja 30
lako lamanja likutshimwitsa, dula, nulitaia iwe: kuti kuli
kwakupindulidwa kwa iwe kuti tshimodzi tsha dziwalo dzako
tshikamwazika, ndimo si tupi lako lonse likamuka m' geena.
Tshinanenedwa anso, Emwe adzatshotsa nkazi watshi, apatse 31
ie lemba la kulekana: koma dinena ndi inu, kuti emwe 32
atshotsa nkazi watshi, kani kwa tshifukwa tsha dama,
apanga ie nkazi wa tshigololo: ndi emwe adzakwata ie
ntawi walekedwa, atshita tshigololo.

Anso, munamva kuti tshinanenedwa ndi awo akali, 33
Usanamiza iwe eka, koma udzatshita kwa Mwini malumbiro
ako: koma dinena ndi inu, Musalumbira konse; kapena 34

ndi kumwamba, tshifuka kuti muli mpando wa Mulungu;
35 kapena ndi pansi, tshifuka kuti pali mpando wa mapazi
atshi; kapena ndi Yerusalem, tshifuka kuti uli mzinda wa
36 Fumu Yotshuka yeikuru. Kapena usalumbira ndi mutu
wako, tshifuka kuti usadziwa ku panga tsisi limodzi
37 lakwiyera kapena lakuda. Koma kunena kwanu kukale,
Ea, ea; Iai, iai: ndimo tshomwe tshiri tshopambana
zimenezi tshiri tsha *wa*mpulupulu.
38 Munamva kuti tshinanenedwa, Diso kwa diso, ndi dzino
39 kwa dzino: koma dinena ndi inu, Musakaniza emwe ali
mpulupulu: koma emwe amenya iwe pa tsaia lako lamanja,
40 tembenuza lina anso kwa ie. Ndimo ngati muntu modzi
afuna ku tengera iwe ku mirandu, ndi ku tshotsa mwinjiro
41 wako, leka ie ku potshera tshopfunda tshako onso. Ndi
42 emwe adzafulumiza iwe ku enda mile limodzi, enda nai'
awiri. Patsa kwa emwe afunsa iwe, ndimo kwa emwe afuna
ku bwereka kwa iwe, usatembenuka.
43 Munamva kuti tshinanenedwa, Udzakonda woiandikila
44 wako, nudzakwiira liwongo lako: koma dinena ndi inu,
Kondani maliwongo anu, ndi pemperani kwa awo omwe
45 azunza inu; monga kuti mungokala ana a Atatu anu emwe
ali m' mwamba: kuti aturutsa dzua latshi pa ampulupulu ndi
46 abwino, natumiza mvula pa odeka ndi osadeka. Kuti ngati
mukonda awo omwe akukondani, mupotshera sekeretso lanje?
47 kodi inde olandira tsong'ko satshita tshointsho? Ndimo
ngati muutsa abali anu oka, mutshita tshiani tshopambana
48 *ena?* kodi inde Mitundu siitshita tshointsho? Ndimo
mudzakala akuta, monga Atatu anu wakumwamba ali
wakuta.

6 Yang'anirani kuti musatshita kudeka kwanu patsogolo pa
antu, ku onedwa ndi awo: kani mupotshera palibe sekeretso
ndi Atatu anu emwe ali m' mwamba.
2 Ndimo ntawi utandizira, usaombera lipenga patsogolo pa
iwe, monga atshinyengo atshita m' masinagoge ndi m'
makwalala, kuti angopotshera kupambana kwa antu.
3 Dinena ndi inu nditu, Analandira sekeretso lao. Koma
ntawi utandizira, usalola dzanja lako lamanzere ku dziwa
4 tshomwe dzanja lako lamanja litshita: kuti matandiziro
ako angokala m' tseri: ndi Atatu ako emwe aona m' tseri
adzasekeretsa iwe.
5 Ndimo ntawi mupempera, musadzakala monga atshinyengo:
kuti akonda ku ima ndi ku pempera m' masinagoge ndi

m' zimphambano za makwalala, kuti angoonedwa ndi antu.
Dinena ndi inu nditu, Analandira sekeretso lao. Koma iwe, 6
ntawi upempera, loa m' tshipinda tshambwalo tshako, ndimo
ntawi unatseka tshitseko, nupempera kwa Atatu ako emwe
ali m' tseri, ndi Atatu ako emwe aona m' tseri adzasekeretsa
iwe. Ndimo m' kupempera musatshita ndi kawiri ndi 7
kawiri kopusa, monga Mitundu itshita: kuti iganiza kuti
idzamvedwa kwa kunena kwambiri kwao. Ndimo musakala 8
ofana ndi imeneyo: kuti Atatu anu adziwa zintu zomwe
muzifuna, patsogolo mumfunsa. Ndimo tshointshi pe- 9
mperani: Atatu atu emwe uli m' mwamba, Liyeretsedwe
dzina lako. Dziko lako lidze. Kufuna kwako kutshitidwe, 10
monga m' mwamba, tshointshi pansi pano. Patsa ife lero, 11
kudia kwa lero. Ndimo kululukira ife mangawa atu, monga 12
ife enso takululukira amangawa atu. Ndimo usatitengere 13
kwa tshinyengo, koma utipulumutse kwa *wa*mpulupulu.
Kuti ngati mukululukira antu matshimo ao, Atatu anu 14
wakumwamba anso adzakululukira inu. Koma ngati 15
musakululukira antu matshimo ao, kapena Atatu anu
wosakululukira matshimo anu.

Koma ntawi muleka kudia, musakala, ofana ndi 16
atshinyengo, ndi nkope za tshisoni: kuti atembenuza nkope
zao, monga kuti aonedwe ndi antu ku leka kudia. Dinena
ndi inu nditu, Analandira sekeretso lao. Koma iwe, ntawi 17
uleka kudia, dzola mutu wako, nusamba nkope yako; kuti 18
usaonedwa ndi antu ku leka kudia, koma ndi Atatu ako
emwe ali m' tseri: ndi Atatu ako, emwe aona m' tseri,
adzasekeretsa iwe.

Musaika kwa inu noka zolemera pansi pano, pomwe 19
tshikululu ndi dzimbiri dzisakaza, ndi pomwe zimbala zibola
naziba: koma ikani kwa inu noka zolemera kumwamba, 20
pomwe kapena tshikululu kapena dzimbiri sidzisakaza, ndi
pomwe zimbala zosabola kapena zosaba: kuti pomwe 21
zolemera zako ziri, apo ntima wako udzali inso. Muni wa 22
tupi uli diso: ndimo ngati diso lako liri limodzi, tupi lako
lonse lidzadzazidwa ndi kuunika. Koma ngati diso lako liri 23
loipa, tupi lako lonse lidzadzazidwa ndi ndima. Ndimo
ngati kuunika komwe kuli mwa iwe kuli ndima, ndima
wambiri bwanje! Palibe muntu adziwa ku imirira ambuye 24
awiri: kuti kapena adzakwiira ndi modzi, ndimo adzakonda
wina; kapena anso adzakala ndi modzi, nadzanyoza wina.
Musadziwa ku imirira ndi Mulungu ndi kulemera. Ndimo 25

dinena ndi inu, Musaganizaganiza ndi moyo wanu, tshiani
mudzadia, kapena tshiani mudzamwa; kapena si kwa tupi
lanu, tshiani mudzabvala. Kodi si moyo wopambana kudia,
26 ndi tupi lopambana nsaru? Onani mbalame za mlengalenga,
kuti zosafesa, kapena zosatema, kapena zosasong'ka m'
zinkokwe; ndimo Atatu anu wakumwamba aziweta. Kodi
27 si inu kwambiri kopambana izo? Ndimo ndani wa inu ndi
kuganizaganiza adziwa ku ong'khetsa nkono umodzi ku
28 nsing'ku watshi? Ndimo muganizaganiza bwanje ndi
nsaru? Ganiza ndi dzikombokombo dza minda, bwanje
29 dzimera; dzosatshita kolimba, kapena dzosapota: koma
dinena ndi inu, kuti inde Solomon m' kupambana kwatshi
konse sanabvaliridwa monga tshimodzi tsha dzimenedzi.
30 Koma ngati Mulungu tshointshi abvalitsa maudzu a munda,
omwe alipo lero, ndi mawa aponyedwa m' stoko, kodi
*wosadzabveka* inu kopambana, O inu a mvanu waung'ono?
31 Ndimo musaganizaganiza, kuti, Tidzadia tshiani? kapena,
Tidzamwa tshiani? kapena, Tidzabvekedwa ndi tshiani?
32 Kuti zintu zonse zimenezi Mitundu ifunira; kuti Atatu anu
wakumwamba adziwa kuti muli ndi kufunidwa ndi zintu
33 zonse zimenezi. Koma funani kopambana dziko latshi, ndi
kudeka kwatshi; ndimo zintu zonse zimenezi zidzaong'khe-
34 tsedwa kwa inu. Ndimo musaganizaganiza kwa mawa:
kuti mawa adzaganizaganiza kwa awo oka. Zambiri ku
siku ziri zoipa zatshi.

7 Musaweruza, kuti musanaweruzidwa. Kuti ndi kuweruza
2 komwe muweruza, mudzaweruzidwa: ndimo ndi muyezo
3 womwe muyeza, tshidzayezedwa kwa inu. Ndimo bwanje
uona tshitolo tshomwe tshiri m' diso la mbali wako, koma
4 usaganiza ndi ntanda womwe uli m' diso lako? Kapena
bwanje udzanena ndi mbali wako, Leka ine ku tshotsa
tshitolo tsha diso lako; ndimo ona, ntanda uli m' diso lako?
5 Watshinyengo iwe, patsogolo tshotsa ntanda kwa diso lako;
ndimo pomwe udzaona bwino ku tshotsa tshitolo kwa diso la
mbali wako.

6 Musapatsa tshomwe tshiri tshoyera kwa agaru, kapena
musaponya maperile anu patsogolo pa ankhumba, kani kapena
aponda awa pansi pa mapazi ao, natembenuka nadula inu.

7 Funsani, ndimo tshidzapatsidwa kwa inu; funani, ndimo
mudzapeza; gogodani, ndimo tshidzatsegulidwa kwa inu:
8 kuti emwe afunsa alandira; ndi emwe afuna apeza; ndi
9 kwa emwe agogoda tshidzatsegulidwa. Kapena muntu uti

ali wa inu, emwe, ngati mwana watshi adzafunsa ie kwa
nkate, kodi adzampatsa mwala; kapena ngati adzafunsa 10
kwa nsomba, kodi adzampatsa njoka? Ndimo ngati inu, 11
muli oipa, mudziwa bwanje ku patsa zolere zabwino kwa
ana anu, bwanje kopambana Atatu anu emwe ali m' mwamba
adzapatsa zintu zabwino kwa omwe amfunsa? Ndimo zintu 12
zonsezomwe mufunakuti antu akatshitakwainu, mutshita inde
tshointsho onso kwa awo: kuti tshimenetshiri maundi aprofeti.

Loani m' tshipata tshopapatiza: kuti tshipata tshiri 13
tshatshikuru, ndi yabwambi iri njira, yomwe itsogolera
kwa kumwazika, ndi ali ambiri omwe aloa mwa itsho.
Tshifuka kuti tshipata tshiri tshopapatiza ndi njira *iri* 14
yeing'ono, yomwe itsogolera ku moyo, ndi owereng'jeka
ali omwe aupeza.

Tshenjerani ndi aprofeti onama, omwe adza kwa inu ndi 15
kubvala kwa nkosa, koma pakati pali zirombo zolusa.
Mudzadziwa awo ndi dzobala dzao. Kodi *antu* atsha 16
magrepe kwa minga, kapena zinkhuyu kwa mitungwi?
Inde tshointshi mitengo yonse yabwino ibala dzobala dza- 17
bwino; koma ntengo woipa ubala dzobala dzoipa. Ntengo 18
wabwino wosadziwa ku bala dzobala dzoipa, kapena ntengo
woipa wosadziwa ku bala dzobala dzabwino. Mitengo yonse 19
yomwe yosabala dzobala dzabwino itemedwa niponye-
dwa m' moto. Ndimo ndi dzobala dzao mudzadziwa awo. 20
Si onse omwe anena ndi ine, Mwini, Mwini, adzaloa m' dziko 21
la kumwamba; koma emwe atshita kufuna kwa Atatu
anga emwe ali m' mwamba. Ambiri adzanena ndi ine m' 22
dzua limenelo, Mwini, Mwini, kodi sitinalosa ndi dzina lako,
ndimo ndi dzina lako sitinaturutsa ademon, ndimo ndi dzina
lako sitinatshita mpamvu zambiri? Ndimo pomwe didza- 23
bvomerera nao Sindinadziwa inu ntawi ina: tshokani kwa
ine, inu nomwe mutshita mpulupulu. Ndimo emwe amva 24
mau anga amene, naatshita, adzafanizidwa ndi muntu
wanzeru, emwe anamanga nyumba yatshi pa tantwe: ndimo 25
mvula inatsika, ndi zigumula zinadza, ndi mpepo zinaomba,
nazimenya pa nyumba imeneyo; ndimo sinagwa: kuti
inazikidwa pa tantwe. Ndi emwe amva mau anga amene, 26
ndimo wosaatshita, adzafanizidwa ndi muntu wopusa, emwe
namanga nyumba yatshi pa ntshenga: ndimo mvula ina- 27
tsika, ndi zigumula zinadza, ndi mpepo zinaomba, nazimenya
pa nyumba imeneyo; ndimo inagwa: ndi kwakukuru kunali
kugwa kwa iyo.

28 Ndimo kunali, ntawi Yesu nata mau amene, antu ambiri
29 nazizwa ndi kupunzitsa kwatshi: kuti anapunzitsa awo
monga *modzi* ali ndi mpamvu, ndimo si monga akulembera ao.
8 Ndimo ntawi anatsika ku piri, antu ambiri anamtsata.
2 Ndimo ona, kunadza kwa ie wakate napembedza ie, kuti,
3 Mwini, ngati ufuna, udziwa kunditsuka. Ndimo naturutsa
dzanja latshi, namtosa, kuti, Difuna; kala wotsukidwa.
4 Ndimo tsopano lino kate latshi linatsukidwa. Ndimo Yesu
anena nai', Yang'ana usauza muntu modzi; koma muka,
udzisonya ku ndzukuru, ndimo tsira ntulo womwe Moses
nauza, kwa kumariza kwa awo.
5 Ndimo ntawi analoa m' Kapernahum, nadza kwa ie ke-
6 nturione, kumpempa, ndimo kuti, Mwini, mwana wanga
alikugona m' nyumba adwala ndi kunjenjemera, apwete-
7 kedwa kwambiri. Ndimo anena nai', Didza didzamtshiritsa.
8 Ndimo kenturione naiang'ka nati, Mwini, sindiri woenera
kuti ukadza pansi pa tshindu langa: koma nena koka mau,
9 ndimo mwana wanga adzatshiritsidwa. Kuti diri inso
mamuna pansi pa mpamvu, diri ndi ankhondo pansi pa ine:
ndimo dinena kwa amene, Muka, ndimo amuka; ndi ku
wina, Idza, ndimo adza; ndi ku kapolo wanga, Tshita
10 tshimenetshi, ndimo atshitshita. Ndimo ntawi Yesu
anamva, nazizwa, nanena ndi omwe anatsata, Dinena ndi
inu nditu, sindapeza mvanu wotshuruka tshointshi, iai, si
11 mwa Sirayeli. Ndimo dinena ndi inu, kuti ambiri adzadza
kwa bvuma ndi kwa zambwe, nadzakala pansi ndi Abraham,
12 ndi Yisake, ndi Yakobi, m' dziko la kumwamba: koma ana
a dziko adzaturutsidwa ku ndima wa kunja: apo padzali
13 kulira nsozi ndi kukukuta kwa mano. Ndimo Yesu nanena
ndi kenturione, Muka; monga unamvana, *tshointshi* tshikale
ndi iwe. Ndi mwana anatshiritsidwa mwa ora limeneli.
14 Ndimo ntawi Yesu nafika m' nyumba ya Petros, naona
15 amai a nkazi wa *Petros*, kugona nadwala malungo. Ndimo
natosa dzanja latshi, ndimo malungo namleka; ndimo
16 nauka, naimirira kwa ie. Ndimo ntawi madzulo anadza,
anatenga kwa ie ambiri anagwidwa ndi ademon: ndimo
naturutsa mizimu ndi mau, natshiritsa onse omwe anali
17 odwala: kuti anangodzazidwa omwe ananenedwa ndi
Yesaya mprofeti, kuti, Ie eka natenga mafoka atu, nanyamula
ntenda zatu.
18 Ndimo ntawi Yesu naona antu ambiri ozungulira ie,
19 nauza ku ng'ka patsidia lina. Ndimo nadza wakulembera

modzi, nanena nai', Mpunzitsi, didzakutsata komwe ung'ka.
Ndimo Yesu anena nai', Ankhandwe ali ndi mapanga, ndi 20
mbalame za mlengalenga *ziri ndi* dzisa; koma Mwana wa
muntu alibe malo ku ika mutu watshi. Ndi wina wa 21
akupunzira nanena nai', Mwini, loleza ine patsogolo ku
ng'ka ku ika atatu anga m' mwanda. Koma Yesu anena 22
nai', Tsata ine; ndimo leka akufa ku ika m' mwanda akufa ao.

Ndimo ntawi analoa m' tshombo, akupunzira atshi 23
natsata ie. Ndimo ona, unauka mondwe woukuru m' 24
nyanja, monga kuti tshombo tshabvundikilidwa ndi ma-
fundi: koma ie anagona tulo. Ndimo nadza kwa ie, 25
nadzutsa ie, kuti, Pulumutsa, Mwini; timwazika. Ndimo 26
anena nao, Muopa ranje, O inu a mvanu waung'ono?
Ndimo nadzuka, nasulumula zimpepo ndi nyanja; ndimo
kunali bata lambiri. Ndimo amuna nazizwa, kuti, Muntu 27
wotani ali amene, kuti inde zimpepo ndi nyanja zimvera ie?

Ndimo ntawi nafika patsidia lina, m' dziko la Agadara, 28
nakomana nai' awiri anagwidwa ndi ademon, kuturuka
mianda, nakaripa kwambiri, monga kuti palibe muntu
anadziwa ku pita pa njira imene. Ndimo ona, napfula, 29
kuti, Tirikutshita tshiani ndi iwe, iwe Mwana wa Mulungu?
kodi udza kuno kutizunza patsogolo pa ntawi? Ndimo 30
linali kutali kwa awo gulu la nkhumba zambiri kueta.
Ndimo ademon napempa ie, kuti, Ngati utiturutsa, tumiza 31
ife kwa gulu la nkhumba. Ndimo nanena nao, Mukani. 32
Ndimo anaturuka, naloa mwa nkhumba: ndimo ona, gulu
lonse linatsika nsanga malo otseruka m' nyanja, nalimwazika
m' madzi. Ndimo awa omwe naziweta natawa, namuka 33
muzinda, nanena zintu zonse, ndi tshomwe tshatshitidwa
ku awa omwe anagwidwa ndi ademon. Ndimo ona, mzinda 34
wonse unaturuka ku komana ndi Yesu: ndimo ntawi naona
ie, napempa *ie* kuti akatshoka miraga yao.

Ndimo naloa m' katshombo, nayambuka, nafika muzinda 9
watshi. Ndimo ona, natenga kwa ie muntu wodwala 2
wonjenjemera, kugona pa kama: ndimo Yesu kuona mvanu
wao nanena ndi wodwala wonjenjemera, Mwana, kala
wosekera; zakwaipa zako zikululukidwa. Ndimo ona, ena 3
a akulembera nanena mwa iwo oka, Amene atukwana.
Ndimo Yesu kudziwa matintu ao nati, Muganiza bwanje 4
zoipa m' mitima yanu? Kuti kuli kopepuka kopambana, 5
ku nena, Zakwaipa zako zikululukidwa; kapena ku ti, Dzuka,
numuka? Koma kuti mudziwe kuti Mwana wa muntu 6

ali ndi mpamvu pansi pano ku kululukira zakwaipa (ndimo
anena ku wodwala wonjenjemera), Dzuka, tukula kama
7 wako, numuka ku nyumba yako. Nadzuka, namuka ku
8 nyumba yatshi. Koma ntawi antu ambiri anaona, naopa,
napambanitsa Mulungu, emwe napatsa mpamvu yotere kwa
antu.

9 Ndimo monga Yesu napita uko, naona muntu, atshedwa
Mateyu, kukala pa malo polandira tsong'ko: ndimo anena
nai', Tsata ine. Ndimo nauka, natsata ie.

10 Ndimo kunali, monga nakala pa kudia m' nyumba, ona,
olandira tsong'ko ambiri ndi ampulupulu nadza nakala
11 pansi ndi Yesu ndi akupunzira atshi. Ndimo ntawi Afarisi
naona, nanena ndi akupunzira atshi, Bwanje Mpunzitsi wanu
12 adia ndi olandira tsong'ko ndi ampulupulu? Koma ntawi
anarnva, nanena, Omwe ali olimba osali ndi kufunidwa ndi
13 sing'anga, koma awo omwe ali odwala. Koma mukani
punzirani tshomwe *tshimene* tshitantauza, Difuna nsisi,
ndimo si nsembe: kuti sindinadza ku itana odeka, koma
ampulupulu.

14 Ndimo adza kwa ie akupunzira a Yohane, kuti, Bwanje
ife ndi Afarisi tileka kudia ntawi zambiri, koma akupunzira
15 ako osaleka kudia? Ndimo Yesu nanena nao, Kodi mapungu
adziwa ku lira, ntawi yomwe wokwati ali nao? koma masiku
adzadza, ntawi wokwati adzatshotsedwa kwa awo, ndimo
16 pomwe adzaleka kudia. Ndimo palibe muntu aika tshigamba
tsha nsaru yatsopano pa maraia akali; kuti tshomwe
tshikwanira itsho tshitshotsa kwa maraia, ndimo tshibo
17 tshatshikuru tshinakala. Kapena *antu* osatsira vinyo
watsopano m' dzikopa dzakali: kani dzikopa dzing'ambika,
ndimo vinyo agabvikiridwa, ndi dzikopa dzitaiika: koma
atsira vinyo watsopano m' dzikopa dzatsopano, ndimo dzonse
dzisungidwa.

18 Ntawi nalankula zintu zimenezi ndi awo, ona, kunadza
woweruza, napembedza ie, kuti, Kabutu kanga kanafa inde
tsopano: koma udze nuika dzanja lako pa iko, ndimo
19 kadzakala ndi moyo. Ndimo Yesu nauka, ndi akupunzira
20 atshi, namtsata. Ndimo ona, nkazi, emwe nadwala ndi
kuka mwazi dzaka kumi ndi dziwiri nadza pambuiu pa ie,
21 natosa ntsheu wa mwinjiro watshi: kuti nanena ndi ntima
watshi, Ngati dingotosa inde mwinjiro watshi, didzatshiri-
22 tsidwa. Koma Yesu kutembenuka ndi kumona nati, Mwana
wankazi, kala wosangalala; mvanu wako wakutshiritsa,

Ndimo nkazi anatshiritsidwa kwa ora limene. Ndimo 23
ntawi Yesu analoa m' nyumba ya woweruza, naona adziteta,
ndi antu ambiri kupanga pokoso, nanena, Piseni malo: kuti 24
kabutu sikanafa, koma kagona. Ndimo naseka ie kwambiri.
Koma ntawi antu ambiri anaturutsidwa, naloa, natenga iko 25
ndi dzanja; ndimo kabutu kanauka. Ndimo mbiri ya 26
tshimene inabuka m' dziko lonse lidya.

Ndimo monga Yesu anapita uko, antu awiri akungu 27
namtsata, napfula, ndimo nati, Kala ndi nsisi pa ife, iwe
mwana wa Davide. Ndimo ntawi nafika m' nyumba, antu 28
akungu nadza kwa ie: ndimo Yesu anena nao, Kodi
mumvana kuti diri ndi mpamvu ku tshita tshimenetshi?
Anena nai', Inde, Mwini. Pomwe natosa maso ao, kuti, 29
Monga mvanu wanu kutshitidwe ndi inu. Ndimo maso ao 30
anatsegulidwa. Ndimo Yesu anauza awa kwambiri, kuti,
Yang'anirani kuti palibe muntu adziwa. Koma anamuka, 31
nabukitsa mbiri yatshi m' dziko lonse lidya.

Ndimo monga anaturuka, ona, kwatengedwa kwa ie 32
muntu wosadziwa ku lankula nagwidwa ndi demon.
Ndimo ntawi demon waturutsidwa, muntu emwe 33
wosadziwa ku lankula nalankula: ndi antu ambiri
nazizwa, kuti, Tshosaonedwa tshointshi mwa Sirayeli ntawi
yapita. Koma Afarisi nati, Aturutsa ademon ndi woweruza 34
wa ademon.

Ndimo Yesu naendaenda mizinda yonse ndi midzi yonse, 35
kupunzitsa m' masinagoge ao, ndi kuuza ivangeli wa dziko,
ndi ku tshiritsa mitundu yonse ya ntenda ndi mitundu yonse
ya kudwala. Koma ntawi naona antu ambiri, namva 36
tshisoni ndi awo, tshifuka kuti anali ofoka ndi obalalika,
monga nkosa zopanda mbusa. Ndimo anena ndi akupu- 37
nzira atshi, Masika ali akuru nditu, koma antshito ali
owereng'jeka. Ndimo pemperani Mwini wa masika, kuti 38
adzatumiza antshito m' masika atshi. Ndimo anaitana kwa 10
ie akupunzira atshi kumi ndi awiri, napatsa awo mpamvu
pa mizimu yosatsuka, ku turutsa iyo, ndi ku tshiritsa
mitundu yonse ya ntenda ndi mitundu yonse ya kudwala.

Ndimo maina a apostile kumi ndi awiri ali amene: 2
Woiamba, Simon, emwe atshedwa Petros, ndi Andreya
mpwatshi; Yakobi *mwana* wa Zebediya, ndi Yohane
mpwatshi; Filipu, ndi Bartolemeyu; Tomas, ndi Mateyu 3
wolandira tsong'ko; Yakobi *mwana* wa Alifeyu, ndi Tadeyu;
Simon ali Mkanane, ndi Yuda Sikariyoti, emwe enso 4

5 anamzonda. Kumi ndi awiri amenewa Yesu natumiza,
nauza awa, kuti,
Musaloa m' njira *imodzi* ya Mitundu, ndimo musaloa
6 m' mzinda umodzi wa Asamariya: koma endani kopambana
7 ku nkosa zosotshera za fuko la Sirayeli. Ndimo monga
muenda, uzani, kuti, Dziko la kumwamba liri pafupi.
8 Tshiritsani odwala, ukitsani akufa, tsukani akate, turutsani
9 ademon: munapotshera kolere, patsani kolere. Musa-
tenga kapena golide, kapena silivere, kapena nkua m'
10 timatumba tanu; kapena tumba kwa olendo *wanu*, kapena
maraia awiri, kapena dzikwakwata, kapena ndodo: kuti
11 wantshito ali woenera kwa kudia kwatshi. Ndimo muzinda
kapena m' mudzi momwe mudzaloa, funsani ndani momo ali
12 woenera; ndimo kalani apo kwa ntawi mung'ka. Ndimo
13 monga muloa m' nyumba, utsani iyo. Ndimo ngati nyumba
iri yoenera, lekani ntendere wanu ku fika pa iyo: koma
ngati si yoenera, lekani ntendere wanu ku bwera kwa inu.
14 Ndimo emwe wosadzalandira inu, kapena wosamva mau
anu, monga mung'ka ku nyumba imene kapena mzinda
15 umene, sansani fumbi la mapazi anu. Dinena ndi inu
nditu, Kudzali kumva pang'ono kwa dziko la Sodom ndi
Gomora m' dzua la kuweruza, kopambana kwa mzinda udya.
16 Ona, ditumiza inu monga zinkosa pakati pa zirombo:
ndimo kalani otshenjera monga zinjoka, ndi osatshimwa
17 monga zinjiwa. Koma tshenjerani ndi antu: kuti adzapereka
inu ku magulu a ankoswe, ndimo m' masinagoge ao adza-
18 kwapula inu; inde ndimo patsogolo pa oweruza ndi mafumu
otshuka mudzatengedwa kwa ine, kwa lomariza kwa awo
19 ndi kwa Mitundu. Koma ntawi akuperekani, musaganiza-
ganiza bwanje kapena tshiani mudzalankula: kuti adza-
patsidwa kwa inu mwa ora limeneli tshomwe mudzalankula.
20 Kuti simuli inu nomwe mulankula, koma Nzimu wa Atatu
21 anu womwe ulankula mwa inu. Ndimo mbali adzapereka
mbali kwa imfa, ndi atate mwana watshi: ndi ana adzauka
22 pa atatu ao ndi amai ao, napetsa awo. Ndimo mudza-
kwiitsidwa ndi antu onse kwa dzina langa: koma iemwe
23 akalabe ku nsonga, emwe adzapulumutsidwa. Koma ntawi
akuzunzani muzinda umene, tawani ku wina: kuti dinena
ndi inu nditu, Musanadzaendaenda mizinda ya Sirayeli, kwa
ntawi Mwana wa muntu anafika.
24 Wakupunzira wosali wopambana mpunzitsi watshi, kapena
25 kapolo wopambana mwini watshi. Kuli kokwanira kwa

wakupunzira kuti akale monga mpunzitsi watshi, ndi kapolo
monga mwini watshi. Ngati anatshedwa mwini wa nyumba
Belzebule, bwanje kopambana *adzatsha* omwe a banja latshi!
Ndimo musaopa awo: kuti palibe kantu kobvundikilidwa, 26
komwe kosadzasonyezedwa; ndimo kobisidwa, komwe kosa-
dzadziwidwa. Tshomwe dikuuzani m' ndima, nenani 27
m' kuunika: ndi tshomwe mumva ndi kutu, uzani pa
matshindu a nyumba. Ndimo musaopa awo omwe apa 28
tupi, koma osadziwa ku pa nzimu: koma kopambana opani
ie emwe adziwa ku mwaza nzimu ndi tupi m' geena. Kodi 29
sikuli mpiningo ziwiri zigulitsidwa kwa fardin limodzi? ndi
palibe imodzi ya izo idzagwa pansi kopanda Atatu anu: koma 30
matsisi nditu a mutu wanu awerengedwa onse. Ndimo 31
musaopa; muli opambana ndi mpiningo zambiri. Ndimo 32
emwe adzabvomera ine patsogolo pa antu, ie didzambvomera
anso patsogolo pa Atatu anga emwe ali m' mwamba. Koma 33
emwe adzakana ine patsogolo pa antu, ie didzamkana anso
patsogolo pa Atatu anga emwe ali m' mwamba.

Musaganiza kuti dinadza ku tumiza ntendere pa dziko: 34
dinadza iai ku tumiza ntendere, koma mpeni wa nkondo.
Kuti dinadza ku kwiitsana muntu ndi atatu atshi, ndi mwana 35
wankazi pa amai atshi, ndi mpongozi pa mpongozi watshi:
ndi maliwongo a muntu *adzakala* omwe a banja latshi. 36
Emwe akonda atatu atshi kapena amai atshi kopambana 37
ine wosali woenera wa ine: ndi emwe akonda mwana
kapena mwana wankazi kopambana ine wosali woenera wa
ine. Ndi emwe wosatukula nkhwitshi yatshi natsata ine, 38
wosali woenera wa ine. Emwe apeza moyo watshi adzau- 39
mwaza; ndi emwe amwaza moyo watshi kwa ine adzaupeza.

Emwe alandira inu alandira ine, ndi emwe alandira ine, 40
alandira ie emwe ananditumiza. Emwe alandira mprofeti 41
m' dzina la mprofeti adzalandira sekeretso la mprofeti; ndi
emwe alandira muntu wodeka m' dzina la muntu wodeka
adzalandira sekeretso la muntu wodeka. Ndi emwe adza- 42
patsa ku mwa ku modzi wa awa ang'ono amene tshiko tsha
madzi ozizira oka, m' dzina la wopunzira, dinena ndi inu
nditu, kulibe kantu kadzamwaza sekeretso latshi.

Ndimo kunali, ntawi Yesu anata ku uza akupunzira atshi 11
kumi ndi awiri, natshoka apo ku punzitsa ndi ku uza m'
mizinda m' ao.

Koma ntawi Yohane anamva m' nyumba ya ndima ntshito 2
za Kristu, natumiza ndi akupunzira atshi, nanena nai', Kodi 3

4 suli emwe adza, kapena tiyang'anire wina? Ndimo Yesu
naiang'ka nanena nao, Mukani, ndimo muuze Yohane zintu
5 zomwe mumva ndi kuona: akungu alandira kuona kwao,
ndi akupunduka miendo aenda, akate atsukidwa, ndi ogonta
amva, ndi akufa aukitsidwa, ndi osauka apotshera ivangeli
6 wauzidwa kwa iwo. Ndimo wodala ali ie, emwe adzapeza
7 palibe tshifukwa tsha kukwiitsa mwa ine. Ndimo monga
amene anamuka, Yesu naamba ku nena ndi antu ambiri ndi
Yohane, Munang'ka m' tshipululu ku ona tshiani? nzengo
8 igwedera ndi mpepo, kodi? Koma munang'ka ku ona
tshiani? muntu wabvala *nsaru* zofewa? Ona, awo omwe
abvala *nsaru* zofewa ali m' nyumba za mafumu otshuka.
9 Koma bwanje munaturuka? ku ona mprofeti? Inde, dinena
10 ndi inu, ndi kwambiri kopambana mprofeti. Amene ali ie,
wa emwe alembedwa,

Ona, ditumiza ntenga wanga patsogolo pa nkope yako,
Emwe adzakonza njira yako patsogolo pa iwe.

11 Dinena ndi inu nditu, Mwa awo omwe abadwa ndi akazi
sanauka wang'kuru wopambana ndi Yohane Mbapatizi:
koma emwe ali wang'ono wopambana mwa dziko la ku-
12 mwamba ali wang'kuru wopambana ndi ie. Ndi kwa masiku
a Yohane Mbapatizi kwa tsopano dziko la kumwamba limva
13 kuipidwa, ndi akuipidwa alitenga ndi kulimbika. Kuti apro-
14 feti onse ndi mau nalosa kwa Yohane. Ndimo ngati mudza-
15 funa ku landira, amene ali Eliya, emwe alinkudza. Emwe
16 ali makutu ku mva, amve. Koma ndi tshiani didza-
faniza fuko limene? Liri lofana ndi ana akala m'
17 mabwalo a maronda, omwe aitana anzao, ndimo ati,
Tinaimba milumbwi kwa inu, ndimo simunabvina; tinalira,
18 ndimo simunapfula. Kuti Yohane nadza kapena sanadia
19 kapena sanamwa, ndimo anena, Ali ndi demon. Mwana
wa muntu nadza kudia ndi kumwa, ndimo ati, Ona, muntu
wosusuka, ndi wokumwa vinyo, mbali wa olandira tsong'ko
ndi ampulupulu! Ndimo nzeru ideketsedwa ndi ntshito zatshi.
20 Ndimo naamba ku dzudzula mizinda, momwe zambiri
zopambana za mpamvu zatshi zinadshitidwa, tshifuka
21 isanatembenuza mitima. Tshaipa kwa iwe, Korazin! tshaipa
kwa iwe, Betsayida! kuti ngati mpamvu zinatshitidwa
mwa Tire ndi Tsidon zomwe zinatshitidwa mwa inu, inaka-
22 tembenuka kali mwa mansansa ndi mapolusa. Koma dinena
ndi inu, kudzali kumva pang'ono kwa Tire ndi Tsidon pa
23 dzua la kuweruza, ndi kwa inu. Ndi iwe, Kapernahum,

kodi udzakalitsidwa kwa kumwamba? udzatsika kwa Hadesi:
kuti ngati mpamvu zinatshitidwa m' Sodom zomwe zinatshi-
tidwa mwa iwe, unakakalabe ku dzua limene. Koma dinena 24
ndi inu, kuti kudzali kumva pang'ono ku dziko la Sodom
m' dzua la kuweruza, kopambana ndi kwa iwe.

Pa ntawi imene Yesu naiang'ka nati, Dinena tshakoma 25
kwa iwe, O Atate, Mwini wa kumwamba ndi pansi, tshifuka
kuti unabisa zintu zimenezi kwa anzeru ndi otshenjera,
nazisonyeza kwa makanda: inde, Atate, kuti tshointsho 26
tshinali tshabwino m' kuona kwako. Zintu zonse zinapere- 27
kedwa kwa ine kwa Atatu anga: ndi palibe modzi adziwa
Mwana, koma Atate; kapena palibe modzi adziwa Atate,
koma Mwana, ndi ie kwa emwe Mwana afuna ku sonyeza
*ie.* Idzani kwa ine, inu nonse nomwe mutshita ndi mule- 28
medwa, ndimo didzakupatsani kupuma. Tengani tshigologolo 29
tshanga pa inu, ndimo punzirani kwa ine; tshifuka kuti
diri wofatsa ndi wosadzitama mutima: ndimo mudzapeza
kupuma kwa mizimu yanu. Kuti tshigologolo tshanga tshiri 30
tshosekesa, ndi katundu wanga ali wopepuka.

Pa ntawi imene Yesu napita pa dzua la sabata pakati pa 12
minda ya dzintu; ndimo akupunzira atshi anamva njala,
naamba ku kadzula ngala za dzintu, nadia. Koma Afarisi, 2
ntawi naona, nanena nai', Ona, akupunzira ako atshita
tshomwe si tshiri tshamau ku tshita pa sabata. Koma 3
nanena nao, Simunawerenga tshomwe Davide natshita,
ntawi anamva njala, ndi awo omwe anali nai'; bwanje 4
naloa m' nyumba ya Mulungu, nadia mikate yoonetsa,
yomwe sikunali kwa mau kwa ie ku dia, kapena kwa omwe
anali nai', koma kwa adzukuru oka? Kapena simunawerenga 5
m' mau, bwanje kuti pa dzua la sabata adzukuru m' tempile
aipitsa sabata, ndimo ali opanda tshimo? Koma dinena ndi 6
inu, kuti modzi wang'kuru wopambana tempile ali pano.
Koma ngati munadziwa tshomwe amene atantauza, Difuna 7
nsisi, ndimo si nsembe, simunakasutsa opanda matshimo.
Kuti Mwana wa muntu ali mwini wa sabata. 8

Ndimo namuka apo, naloa m' sinagoge mwao: ndimo 9, 10
ona, muntu ali ndi dzanja louma. Ndimo namfunsa, kuti,
Kodi kuli kwamau ku tshiritsa pa dzua la sabata? monga
kuti anangotshula ie. Ndimo nanena nao, Muntu uti adzali 11
mwa inu, emwe adzali ndi nkosa imodzi, ndimo ngati imene
igwa m' dzenje pa dzua la sabata, kodi sadzaigwira, nadzai-
turutsa? Ndimo bwanje muntu ali wabwino wopambana 12

nkosa! Monga kuti kuli kwamau ku tshita bwino pa dzua
13 la sabata. Ndimo anena ndi muntu, Turutsa dzanja lako.
Ndimo naliturutsa; ndimo linatshiritsidwa lolimba, monga
14 lina. Koma Afarisi naturuka, nafunsana pa ie, bwanje
15 angomwaza ie. Ndimo Yesu kudziwitsa napambuka apo:
16 ndi ambiri namtsata; ndimo natshiritsa awo onse, nauza
17 awa kuti osakadziwitsa ie: kuti kunangodzazidwa komwe
kwanenedwa mwa Yesaya mprofeti, kuti,

18 Ona, mwana wanga emwe dasang'ka;
Wokondedwa wanga mwa emwe nzimu wanga usekera bwino:
Didzaika Nzimu wanga pa ie,
Ndimo adzauza kuweruza kwa Mitundu.
19 Sadzadana, kapena sadzapfula;
Kapena muntu modzi sadzamva liu latshi mwa makwalala.
20 Nzengo yotswanya sadzaitshola,
Ndi lini lomwe lifuka sadzalizima,
Kwa ntawi atumiza kuweruza kwa kupambana.
21 Ndimo m' dzina latshi Mitundu idzalingalira.

22 Ndimo natengedwa kwa ie modzi wogwidwa ndi demon,
wakungu ndi wosadziwa ku lankula: namtshiritsa, monga
23 kuti wosadziwa ku lankula, nalankula naona. Ndimo antu
onse ambiri nazizwa, nati, Kodi amene ali mwana wa Davide?
24 Koma ntawi Afarisi anamva, nanena, Muntu amene wosa-
turutsa ademon, koma ndi Belzebule woweruza wa ademon.
25 Ndimo kudziwa matintu ao nanena nao, Maiko onse agawidwa
pa oka atengedwa ku bwinja; ndi mizinda yonse kapena
26 nyumba *zonse* zigawidwa pa zoka sizidzakala: ndimo ngati
Satana aturutsa Satana, agawidwa pa eka; ndimo dziko latshi
27 lidzakala bwanje? Ndimo ngati ine ndi Belzebule diturutsa
ademon, ana anu aturutsa awo ndi ani? Ndimo adzakala
28 oweruza anu. Koma ngati ine ndi Nzimu wa Mulungu diturutsa
29 ademon, pomwe dziko la Mulungu linadza pa inu. Kapena
bwanje modzi adziwa ku loa m' nyumba ya *muntu* wolimba,
ku ononga zintu zatshi, kani poiamba amange *muntu* wolimba?
30 ndimo pomwe adzaononga nyumba yatshi. Iemwe wosali
ndi ine ali pa ine; ndi iemwe wosakung'ka ndi ine ataia.
31 Ndimo dinena ndi inu, Mpulupulu zonse ndi matukwano
zidzakululukiridwa kwa antu; koma tukwano pa Nzimu
32 losadzakululukiridwa. Ndimo emwe adzanena liu pa Mwana
wa muntu, lidzakululukiridwa ie; koma emwe adzanena pa

Nzimu Woyera, kosadzakululukiridwa ie, kapena mwa ku-
gonera kumene, kapena mwa kumene komwe kulinkudza.
Kapena pangani mtengo wabwino, ndi dzobala dzatshi 33
dzabwino; kapena pangani mtengo woipa, ndi dzobala
dzatshi dzoipa: kuti mtengo udziwidwa ndi dzobala dzatshi.
Inu fuko la zinjoka, bwanje inu, muli oipa, mudziwa ku 34
lankula zintu zabwino? kuti kwa zambiri za ntima nkamwa
munena. Muntu wabwino kwa kulemera kwabwino kwatshi 35
aturutsa zintu zabwino: ndi muntu woipa kwa kulemera
koipa kwatshi aturutsa zintu zoipa. Koma dinena ndi inu, 36
kuti mau onse olesi omwe antu adzalankula, adzawerengera
ndi amene m' dzua la kuweruza. Kuti ndi mau ako udza- 37
deketsedwa, ndimo ndi mau ako udzasutsidwa.

Ndimo ena a akulembera ndi a Afarisi naiang'ka ie, kuti, 38
Mpunzitsi, tifuna ku ona tshizindikilo kwa iwe. Koma 39
naiang'ka nanena nao, Fuko loipa ndi latshigololo lifunira
tshizindikilo; ndimo palibe tshizindikilo tshidzapatsidwa
kwa ilo koma tshizindikilo tsha Yona mprofeti: kuti monga 40
Yona anali madzua atatu ndi masiku atatu m' mimba mwa
hwele; tshointshi Mwana wa muntu adzakala madzua atatu
ndi masiku atatu muntima mwa dziko. Amuna a Ninive 41
adzaima mwa kuweruza ndi fuko limene, nadzalisutsa:
tshifuka kuti natembenuka pa kuuza kwa Yona; ndi ona,
wang'kuru ndi Yona ali pano. Fumu yeikazi ya kumwela 42
idzauka mwa kuweruza ndi fuko limene, nidzalisutsa: kuti
inadzera kutali kwa dziko ku mva nzeru za Solomon; ndimo
ona, wang'kuru wopambana ndi Solomon ali pano. Koma 43
nzimu wosatsuka, ntawi unaturuka mwa muntu, upita
mwa malo opanda madzi kufuna kupuma, ndimo usapeza
iko. Ndimo uti, Dibwera ku nyumba yanga yomwe 44
dinadzera; ndimo ntawi unafika, uipeza yopanda kantu,
yosesedwa, ndi yofotokozedwa. Ndimo ung'ka, nutenga 45
ndi iwo woka mizimu isanu ndi iwiri ina yoipa yopambana
iwo woka, niloa, nikala umo: ndi makalidwe akutungo a
muntu ameneyo akala oipa opambana oamba. Inde
tshointsho kudzali inso ku fuko limene loipa.

Ntawi analikulankula ndi antu ambiri, ona, amai atshi 46
ndi abali atshi naima kunja, kufuna ku lankula ndi ie.
Ndimo modzi nanena ndi ie, Ona, amai ako ndi abali ako 47
aima kunja, kufuna ku lankula ndi iwe. Koma naiang'ka 48
nanena ndi emwe anamuza, ndani ali amai anga? ndimo
ndani ali abali anga? Ndimo naturutsa dzanja latshi kwa 49

akupunzira atshi, nati, Ona, amai anga ndi abali anga!
50 Kuti emwe adzatshita kufuna kwa Atatu anga emwe ali
m' mwamba, iemwe ali mpwanga ndi mlongo wanga, ndi
amai.

13 M' dzua limene Yesu naturuka m' nyumba, nakala mbali
2 mwa nyanja. Ndimo anasong'kanidwa kwa ie antu ambiri,
monga kuti naloa m' tshombo, nakala; ndi antu onse ambiri
3 naima pa doko. Ndimo nalankula kwa awo zintu zambiri
4 ndi mafanizo, kuti, Ona, wofesa naturuka ku fesa; ndimo
monga analikufesa, *mbeu* ina inagwa mbali mwa njira ndi
5 mbalame zinadza zinaidia: ndimo ina inagwa pa malo
atantwe, pomwe siinapotshera ntaka yambiri: ndimo
tsopano lino inamera, tshifuka siinapotshera ntaka yakuya;
6 ndimo ntawi dzua linali kumwamba, inanyalitsidwa, ndimo
7 tshifuka inali yopanda ntsitsi, inakwinyata. Ndimo ina
inagwa pa minga; ndimo minga inamera, nikwinyatitsa
8 iyo: koma ina inagwa pa ntaka yabwino, nibala dzobala,
ina makumi okaoka kumi, ina makumi asanu ndi modzi, ina
9 makumi atatu. Emwe ali makutu, amve.
10 Ndimo akupunzira nadza, nanena nai', Bwanje ulankula
11 nao ndi mafanizo? Ndimo naiang'ka nanena nao, Kwa inu
kupatsidwa ku dziwa kusadziwika kwa dziko la kumwamba,
12 koma ku awo kusadzapatsidwa. Kuti emwe apotshera, kwa
ie adzapatsidwa, ndimo adzapotshera kwambiri: koma emwe
wosapotshera, kwa ie tshidzatshotsedwa inde tshomwe atshi-
13 potshera. Ndimo dilankula nao m' mafanizo; tshifuka
14 kuona osaona, ndi kumva osamva, kapena osamvetsa. Ndi
kwa iwo kunadzaza kulosa kwa Yesaya, komwe kunena,

Ndi kumva mudzamva, ndimo musadzamvetsa konse;
Ndi kuona mudzaona, ndimo musadzaonetsa konse:
15 Kuti mitima ya antu amene inakala yolimba,
Ndi makutu ao ali ogonta,
Ndi maso ao anatseka;
Kani kapena akaona ndi maso ao,
Ndimo akamva ndi makutu ao,
Ndimo akamvetsa ndi mitima yao,
Ndimo akatembenuka anso,
Ndimo dikatshiritsa awo.

16 Koma odala ali maso anu, kuti aona; ndi makutu anu, kuti
17 amva. Kuti dinena ndi inu nditu, kuti aprofeti ambiri ndi antu
odeka nafuna ku ona zintu zomwe muona, ndimo sanazions;
18 ndi ku mva zintu zomwe mumva, ndimo sanazimva. Ndimo

imvani fanizo la wofesa. Ntawi muntu modzi amva 19
mau a dziko, ndimo wosamvetsa, *pomwe* adza *wa*mpulupulu,
natshotsa omwe anafesedwa mutima mwatshi. Amene ali
emwe anafesedwa mbali mwa njira. Ndimo emwe ana- 20
fesedwa pa malo atantwe, amene ali emwe amva mau,
ndimo tsopano lino ndi tshimwemwe alandira; koma 21
wosapotshera ntsitsi mwa ie eka, koma akalabe kwa ntawi;
ndimo ntawi tshisoni kapena sautso ziuka tshifuka tsha mau,
tsopano lino akwiitsa. Ndimo emwe anafesedwa mwa minga, 22
amene ali emwe amva mau; ndi ganizo la kugonera, ndi
tshinyengo tsha kulemera, zikwinyatitsa mau, ndimo wosa-
bala kantu. Ndimo emwe anafesedwa pantakayabwino, amene 23
ali emwe amva mau, ndimo amvetsa; emwe nditu abala
dzobala, ndimo aturutsa, ena makumi okaoka kumi, ena
makumi asanu ndi modzi, ena makumi atatu.

Fanizo lina naika patsogolo pa awo, kuti, Dziko la 24
kumwamba lifanizidwa ndi muntu emwe nafesa mbeu
yabwino m' munda mwatshi: koma ntawi antu nagona, 25
liwongo latshi linadza linafesa anasongole enso mwa trigu,
linamuka. Koma ntawi kwata linaturuka, linamasula 26
dzobala, pomwe nasonyeza anasongole enso. Ndimo 27
akapolo a mwini wa nyumba nadza nanena nai', Fumu,
kodi sunafesa mbeu yabwino m' munda wako? kwa kuti
unali ndi anasongole? Ndimo nanena nao, Muntu emwe 28
ali liwongo latshita tshimenetshi. Ndimo akapolo anena
nai', Kodi ndimo ufuna kuti ting'ke kwasankula? Koma 29
anena, Iai; kani kapena ntawi musankula anasongole mudza-
zula trigu ndi awo. Lekani zonse ku kulira pa modzi kwa 30
masika: ndimo m' ntawi ya masika didzauza otema, Sanku-
lani patsogolo anasongole, naamanga m' mitolo ku otsha
awo: koma kung'khani trigu ku nkokwe yanga.

Fanizo lina naika pa awo, kuti, Dziko la kumwamba liri 31
lofana mpetshe ya mostade, yomwe muntu natenga, nafesa
m' munda mwatshi: yomwe nditu iri yeing'ono yopambana 32
ya mbeu zonse; koma ntawi inakula, iri yeikuru yopambana
mpobvu, ndimo ikala mtengo, monga kuti mbalame za
mlengalenga zidza ndi zikala pa ntambi pa iwo.

Fanizo lina nalankula nao; Dziko la kumwamba liri 33
lofana ndi fumba, yomwe nkazi natenga, nabisa m' miezo
itatu ya ufa, kwa ntawi wonse unatupitsidwa.

Zintu zonse zimenezi Yesu nazilankula m' mafanizo kwa 34
antu ambiri; ndi lopanda fanizo sanalankula kantu kwa

35 awo: monga kuti anangodzazidwa omwe ananenedwa mwa
mprofeti, kuti,

Didzatsegula nkamwa mwanga ndi mafanizo;
Didzatshula zintu zinabisidwa kwa kuzika kwa dziko.

36 Ndimo nasia antu ambiri, naloa m' nyumba: ndi akupunzira
atshi nadza kwa ie, kuti, Utiuze fanizo la anasongole a
37 munda. Ndimo naiang'ka nanena, Iemwe afesa mbeu
38 yabwino ali Mwana wa muntu; ndi munda uli dziko; ndi
mbeu yabwino, amene ali ana a dziko; ndimo anasongole
39 ali ana a *wa*mpulupulu; ndi liwongo lomwe linafesa awo liri
diabolos: ndi masika ali kuta kwa kugonera; ndi otema ali
40 anjelo. Ndimo monga anasongole asankulidwa naotshedwa
41 ndi moto; tshointshi padzali pa kuta pa kugonera. Mwana
wa muntu adzatumiza anjelo atshi, ndimo adzasankula kwa
dziko latshi zintu zonse zomwe zikwiitsa, ndi omwe atshita
42 mpulupulu, ndimo adzaataia m' ng'anjo ya moto: apo kudzali
43 maliro ndi kukukuta mano. Pomwe odeka adzawala monga
dzua m' dziko la Atatu ao. Emwe ali makutu, amve.

44 Dziko la kumwamba liri lofana ndi kulemera kobisidwa
m' munda: komwe muntu napeza, nabisa; ndimo m' tshi-
mwemwe tshatshi ang'ka nagulitsa zonse zomwe ali nazo,
nagula munda umene.

45 Anso, dziko la kumwamba liri lofana ndi muntu emwe ali
46 wamaronda kufuna maperile abwino: ndimo anapeza perile
limodzi la ntengo wapatali, naug'ka nagulitsa zonse zomwe
ali nazo, naligula.

47 Anso, dziko la kumwamba liri lofana ndi ukonde, womwe
unaponyedwa m' nyanja, nusong'ka za mitundu yonse:
48 womwe, ntawi unadzazidwa, nakoka pa doko; ndimo nakala
pansi, nasankula zabwino m' dziwira, koma nataia zoipa.
49 Tshointsho kudzali pa kuta pa kugonera: anjelo adzaturuka,
50 nadzagawa oipa kwa odeka, nadzataia m' ng'anjo ya moto:
apo kudzali maliro ndi kukukuta mano.

51 Kodi munadziwitsa zintu zonse zimenezi? Anena nai',
52 Inde. Ndimo nanena nao, Ndimo akulembera onse omwe
anapangidwa akupunzira kwa dziko la kumwamba ali ofana
ndi muntu emwe ali mwini wa nyumba, emwe aturutsa kwa
zolemera zatshi, zintu zatsopano ndi zakali.

53 Ndimo kunali, ntawi Yesu anata mafanizo amenewa,
54 namuka uko. Ndimo kufika m' dziko latshi napunzitsa awo
m' sinagoge mwao, monga kuti anazizwa, nati, Kuti muntu
55 amene ali ndi nzeru zimenezi, ndi mpamvu zimenezi? Kodi si

amene mwana wa misiri wa mitengo? kodi si amai atshi
atshedwa Mariya? ndi abali atshi, *kodi si* Yakobi, ndi Yosefe,
ndi Simon, ndi Yuda? Ndi alongo atshi, kodi si onse ali ndi 56
ife? Ndimo kuti pomwe muntu amene ali nazo zintu zonse
zimene? Ndimo nakwiitsidwa ndi ie. Koma Yesu nanena 57
nao, Mprofeti sali wopanda ulemu, kani m' dziko latshi, ndi
m' nyumba mwatshi. Ndimo apo sanachita .mpamvu zambiri 58
tshifuka tsha kusamvana kwao.

Pa ntawi imene Herode woweruza wa tshinai, anamva 14
mbiri ndi Yesu, nanena ndi ana atshi, Amene ali Yohane 2
Mbapatizi; anaukiridwa kwa akufa; ndimo tshointsho
mpamvu zimene zitshita mwa ie. Kuti Herode anagwira 3
Yohane, nammanga, namwika m' nyumba ya ndima kwa
Herodiya, nkazi wa njiratshi Filipu. Kuti Yohane nanena 4
nai', Sitshiri tshamau kwa iwe uli nai'. Ndimo ntawi nafuna 5
kumpa, naopa antu ambiri, tshifuka naganiza ie monga
mprofeti. Koma ntawi dzua lobadwa la Herode linafika, 6
butu la Herodiya linabvina pakati, nalisekeretsa Herode.
Pomwe nalonjezana ndi lumbiro kulipatsa tshomwe likafunsa. 7
Ndimo ilo, kukang'kaziridwa ndi amai atshi, liti, Undipatse 8
kuno m' mbale yeikuru mutu wa Yohane Mbapatizi. Ndimo 9
fumu yotshuka inamva tshisoni; koma kwa malumbiro atshi,
ndi kwa omwe nadia nai', nauuza ku patsidwa; ndimo 10
natumiza, nadula mutu wa Yohane m' nyumba ya ndima.
Ndimo mutu watshi unatengedwa m' mbale yeikuru, 11
nupatsidwa kwa butu: ndimo ilo linautenga kwa amai atshi.
Ndimo akupunzira atshi nadza, natukula ntembo, nauika 12
m' mwanda; ndimo nang'ka nauza Yesu.

Ndimo ntawi Yesu anamva, natshoka apo ndi tshombo, 13
ku tshipululu oka: ndimo ntawi antu ambiri anamva *ndi*
*kumene* namtsata ndi miendo ku mizinda. Ndimo naturuka, 14
naona antu ambiri, namva tshisoni mutima ku awo, ndimo
natshiritsa odwala ao. Ndimo ntawi madzulo anadza, 15
akupunzira nadza kwa ie, kuti, Malo ali tshipululu, ndimo
ntawi tsopano yapita; tshotsa antu ambiri, monga kuti
angong'ka m' midzi, nagula kudia kwa awo oka. Koma 16
Yesu nanena nao, Osali ndi kufunidwa ku muka; patsani
awo ku dia. Ndimo anena nai', Tiri nazo pano zoka mikate 17
isanu, ndi nsomba ziwiri. Ndimo nati, Tengani izo kuno 18
kwa ine. Ndimo nauza antu ambiri ku kala pansi pa 19
maudzu; ndimo natenga mikate isanu, ndi nsomba ziwiri
ndi kuyang'ana kumwamba, nadalitsa, naswa napatsa mikate

20 kwa akupunzira, ndi akupunzira kwa antu ambiri. Ndimo
onse anadia, nakuta: ndimo natola zomwe zotsala za zosweka,
21 mitanga kumi ndi iwiri yodzaza. Ndimo awa omwe anadia
anali kwa antu mazousan asanu, ndi akazi ndi ana kopa-
mbana.
22 Ndimo tsopano lino nafulumiza akupunzira ku loa m'
tshombo, ndi ku pita patsogolo pa ie patsidia lina, kwa
23 ntawi akatshotsa antu ambiri. Ndimo pambuiu anatshotsa
antu ambiri, nakwera pa piri ie eka ku pempera: ndimo
24 ntawi madzulo anadza, anali apo eka. Koma tshombo
tshinali tsopano pakati pa nyanja, tshinandengumidwa ndi
25 mafundi; kuti mpepo inalinkudza patsogolo. Ndimo m'
kudikira kwatshinai kwa usiku nafika kwa iwo, kuenda pa
26 nyanja. Ndimo ntawi akupunzira namona kuenda pa
nyanja, nantuntumiridwa, kuti, Uli nzukwa; ndimo napfula
27 ndi kuopa. Koma tsopano lino Yesu nalankula nao, kuti,
28 Kalani osekera; diri ine; musaopa. Ndimo Petros naiang'ka
ie nati, Mwini, ngati uli iwe, uza ine ku dza kwa iwe pa
29 madzi. Ndimo nati, Idza. Ndimo Petros natsika m'
30 tshombo, naenda pa madzi, ku fika kwa Yesu. Koma ntawi
naona mpepo, naopa; ndimo kuamba ku bira, napfula, kuti,
31 Mwini, pulumutsa ine. Ndimo tsopano lino Yesu naturutsa
dzanja latshi, namgwira, ndimo anena nai', O iwe wa mvanu
32 waung'ono, bwanje usamvana? Ndimo ntawi analoa m'
33 tshombo, mpepo inaleka. Ndimo awa omwe anali m' tshombo
nampembedza, kuti, Ndi nteradi uli Mwana wa Mulungu.
34 Ndimo ntawi anayambuka, nafika ku ntunda, ku Genesa-
35 rete. Ndimo ntawi antu a malo amene nadziwa ie, natumiza
ku dziko lonse limenelo lozungulira, natenga kwa ie onse
36 omwe anali odwala: ndimo napempa ie kuti anangotosa
koka mtsheu wa mwinjiro watshi: ndimo monga ambiri
monga natosa anatshiritsidwa.

15 Ndimo adza kwa Yesu ku Yerusalem Afarisi ndi akule-
2 mbera, kuti, Bwanje akupunzira ako aswa mwambi wa akuru?
3 kuti osasamba manja ao ntawi adia nkate. Ndimo naiang'ka
nanena nao, Bwanje muswa anso mau a Mulungu tshifuka
4 tsha mwambi wanu? Kuti Mulungu nati, Lemekeza atatu
ako ndi amai ako: ndimo, Iemwe anena zoipa ndi atatu atshi
5 kapena amai atshi, afe imfa. Koma munena, Emwe adza-
nena ndi atatu atshi kapena ndi amai atshi, Tshimene ndi
tshomwe unangopindulidwa ndi ine tshipatsidwa *kwa*
6 *Mulungu;* sadzalemekeza atatu atshi. Ndimo munapanga

mau a Mulungu tshabe tshifuka tsha mwambi wanu.
Inu atshinyengo, Yesaya nalosa bwino ndi inu, kuti, 7

Antu amene alemekeza ine ndi milomo yao; 8
Koma mitima yao iri kutali kwa ine.
Koma kwautsiru andipembedza, 9
Kupunzitsa *monga* mapunzitso *ao*, mau a antu.

Ndimo naitana kwa ie antu ambiri, nanena nao, Imvani, ndimo 10
mvetsani: Si tshomwe tshiloa m' nkamwa tshidetsa muntu; 11
koma tshomwe tshituruka kwa nkamwa, tshimene tshidetsa
muntu. Ndimo nadza akupunzira, nanena nai', Kodi udziwa 12
kuti Afarisi anakwiitsidwa, ntawi anamva mau amene?
Koma naiang'ka nati, Mimera yonse yomwe Atatu anga 13
wakumwamba sanaoka, idzazulidwa. Lekani awa; ali 14
atsatsogolo akungu. Ndimo ngati akungu atsogola akungu,
onse awiri adzagwa m' dzenje. Ndimo Petros naiang'ka 15
nanena nai', Uza ife fanizo. Ndimo nati, Kodi muli inso 16
inde tsopano opanda kudziwa? Kodi simudziwitsa, kuti 17
tshomwe tshiloa m' nkamwa tshipita m' mimba, ndimo
tshiturutsidwa poonyera? Koma zintu zomwe zituruka pa 18
nkamwa zituruka kwa ntima; ndimo zidetsa muntu.
Kuti kwa ntima zituruka maganizo oipa, ambanda, zigololo, 19
madama, zimbala, masinjiriro, matukwano: zimenezi ziri 20
zintu zomwe zidetsa muntu: koma ku dia ndi manja
osasamba sikudetsa muntu.

Ndimo Yesu nang'ka uko, nabwerera ku malo a Tire ndi 21
Tsidon. Ndimo ona, nkazi Wakanane naturuka miraga 22
imeneyo, napfula, kuti, Kala ndi nsisi ndi ine, O Mwini,
mwana wa Davide; butu langa ligwidwa kolimba ndi demon.
Koma sanaiang'ka nai' mau. Ndimo akupunzira atshi nadza 23
nampempa, kuti, Tshotsa ie; kuti apfula pambuiu pa ife.
Koma naiang'ka nanena, Sindinatumidwa koma kwa nkosa 24
zosotshera za nyumba ya Sirayeli. Koma nadza napembe- 25
dza ie, kuti, Mwini tangata ine. Koma naiang'ka nati, Si 26
tshabwino ku tenga nkate wa ana ndi kuutaia kwa agaru.
Koma nanena, Inde Mwini: kuti inde agaru adia nyenyeswa 27
zomwe zigwa pa gome la ambuiye ao. Ndimo Yesu naiang'ka 28
nanena nai', O nkazi, ukuru uli mvanu wako: tshikale ndi
iwe inde monga ufuna. Ndimo butu latshi linatshiritsidwa
kwa ora limenelo.

Ndimo Yesu nang'ka uko, nadza mbali mwa nyanja ya 29
Galileya; ndimo nakwera m' piri, nakala pansi apo. Ndimo 30
antu ambiri nadza kwa ie. anali nao opunduka miendo,

akungu, osalankula, opunduka, ndi ambiri ena, naaika pa
31 mapazi atshi; natshiritsa awo: monga kuti antu ambiri
nazizwa, ntawi naona osalankula kulankula, opunduka olimba,
ndi opunduka miendo kuenda, ndi akungu kuona: ndimo
napambanitsa Mulungu wa Sirayeli.
32 Ndimo Yesu naitana kwa ie akupunzira atshi, nati, Diri
ndi tshisoni mutima ndi antu ambiri, tshifuka akalabe ndi
ine tsopano masiku atatu ndimo osapotshera kantu ku dia:
ndimo sindifuna ku tshotsa awo opanda kudia, kani kapena
33 afoka pa njira. Ndimo akupunzira anena nai', Kuti tika-
potshera mikate monga yambiri m' tshipululu, monga kuti
34 kukutitsa antu ambiri otere? Ndimo Yesu anena nao, Mi-
kate ingati muli naiyo? Ndimo nanena, Isanu ndi iwiri, ndi
35 nsomba zowereng'jeka zazing'ono. Ndimo nauza antu ambiri
36 ku kala pansi; ndimo natenga mikate isanu ndi iwiri ndi
zinsomba; nati tshakoma naswa, napatsa ku akupunzira, ndi
37 akupunzira kwa antu ambiri. Ndimo onse anadia, nakuta:
natola zomwe zotsala za nyenyeswa mitanga isanu ndi iwiri
38 yodzaza. Ndimo omwe anadia anali amuna mazousan anai,
39 ndi akazi ndi ana kopambana. Ndimo natshotsa antu
ambiri, naloa m' tshombo, nadza ku maliri a Magadan.
16 Ndimo Afarisi ndi Asadusi nadza, ndi kumyesa nafunsa
2 ie ku sonyeza awo tshizindikilo kwa kumwamba. Koma
naiang'ka nanena nao, Ntawi ali madzulo, muti, *Kudzakala*
3 ntawi yabwino: kuti mlengalenga uli wofira. Ndimo ma-
mawa, *Kudzakala* ntawi yoipa lero: kuti mlengalenga uli
wofira ndi wotumbirira. Mudziwa bwanje ku werenga
nkope ya mlengalenga; koma musadziwa *ku werenga* zizindi-
4 kilo za zintawi. Fuko loipa ndi latshigololo lifuna tshizindi-
kilo; ndimo tshizindikilo palibe tshidzapatsidwa kwa ilo,
koma tshizindikilo tsha Yona. Ndimo nasia awo, namuka.
5 Ndimo akupunzira anafika kutsidia lina naiwala ku tenga
6 mikate. Ndimo Yesu nanena nao, Yang'anirani ndi tshenje-
7 rani ndi fumba ya Afarisi ndi ya Asadusi. Ndimo nauzana
8 mwa iwo oka, kuti, Sitinatenga mikate. Ndimo Yesu kutshi-
dziwitsa nati, O inu a mvanu waung'ono, bwanje muuzana
9 inu noka, tshifuka kuti musali ndi mikate? Kodi simuna-
dziwitsa, kapena simunakumbukila mikate isanu ya mazousan
10 asanu, ndimo mitanga ingati munatola? Kapena mikate
isanu ndi iwiri ya mazousan anai ndi mitanga ingati
11 munatola? Bwanje simudziwitsa kuti sindinanena ndi inu
ndi mikate? Koma tshenjerani ndi fumba ya Afarisi ndi

ya Asadusi. Ndimo anadziwa bwanje kuti wosauza awa 12
ku tshenjera ndi fumba ya mikate, koma ndi kupunzitsa
kwa Afarisi ndi kwa Asadusi.

Ndimo ntawi Yesu anadza ku malo a Kesareya wa Filipu, 13
nafunsa akupunzira atshi kuti, Antu anena kuti Mwana wa
muntu ali ani? Ndimo nati, Ena *ati* Yohane Mbapatizi; ena, 14
Eliya: ndi ena, Yeramiya, kapena modzi wa aprofeti. Anena 15
nao, Koma munena kuti diri ani? Ndimo Simon Petros 16
naiang'ka nati, Uli Kristu, Mwana wa Mulungu wamoyo.
Ndimo Yesu naiang'ka nanena nai', Wodala uli iwe, Simon 17
Barayona: kuti nyama ndi mwazi sizinatshisonyeza kwa
iwe, koma Atatu anga emwe ali m' mwamba. Ndimo 18
dinena anso ndi iwe, kuti uli Petros, ndi pa tantwe limene
didzamanga eklesia langa; ndimo dzipata dza Hadesi
dzosadzapambana pa ilo. Didzakupatsa fungulu za dziko 19
la kumwamba: ndi tshomwe udzamanga pansi pano tshidza-
mangidwa kumwamba: ndi tshomwe udzamasula pansi pano
tshidzamasulidwa kumwamba. Pomwe nauza akupunzira 20
kuti sakauza muntu kuti anali Kristu.

Kwa ntawi imeneyo Yesu naamba ku sonyeza kwa aku- 21
punzira atshi, bwanje kuti akanang'ka ku Yerusalem, ndimo
ku mva zintu zambiri ndi akuru ndi adzukuru akuru ndi
akulembera, ndi ku pedwa, ndi ku dzukitswa pa siku
latshitatu. Ndimo Petros anamtenga, naamba kumsulumula, 22
kuti, Kuli kutali kwa iwe Mwini: tshimene sitshidzali palibe
ntawi kwa iwe. Koma natembenuka, nanena ndi Petros, 23
Pita pambuiu pa ine, Satana: uli kwiitso kwa ine: kuti
usasamala zintu za Mulungu, koma zintu za antu. Ndimo 24
Yesu nanena ndi akupunzira atshi, Ngati muntu modzi
afuna ku dza pambuiu panga, adzikanize, ndimo anyamule
nkhwitshi yatshi, nanditsate. Kuti emwe afuna ku pulu- 25
mutsa moyo watshi adzaumwaza: ndi emwe adzamwaza
moyo watshi kwa ine adzaupeza. Kuti bwanje muntu 26
adzapindulidwa, ngati adzalandira dziko lonse, ndimo nasinta
moyo watshi? kapena tshiani muntu adzapatsa m' kusintana
kwa moyo watshi? Kuti Mwana wa muntu adzadza m' 27
kupambana kwa Atatu atshi ndi anjelo atshi; ndimo pomwe
adzabweza ku antu onse kwa ntshito zao. Dinena ndi inu 28
nditu, Alipo ena a omwe aima pano, omwe sadzalawa nditu
imfa, kwa ntawi aona Mwana wa muntu kudza m' dziko latshi.

Ndimo pambuiu masiku asanu ndi limodzi Yesu atenga 17
ndi ie Petros, ndi Yakobi, ndi Yohane mpwatshi, nakweretsa

2 awo pa piri lalitali iwo oka: ndimo nasandulikidwa patsogolo
pa awo: ndimo nkope yatshi inawala monga dzua, ndi nsaru
3 zatshi zinayera monga kuunika. Ndimo ona, kunasonyeza
4 ku awa Moses ndi Eliya kulankula nai'. Ndimo Petros
naiang'ka, nanena ndi Yesu, Mwini, tshiri tshabwino kwa ife
tiri kuno: ngati ufuna, didzamanga pano misasa itatu;
umodzi kwa iwe, ndi umodzi kwa Moses, ndi umodzi kwa
5 Eliya. Ntawi analikulankula, ona, mtambo woyera una-
pimba awa: ndimo ona, liu mutambo, kunena, Amene ali
Mwana wanga wondikonda, ndi emwe disekera bwino;
6 imvani ie. Ndimo ntawi akupunzira analimva, nagwa pa
7 nkope pao, naopa kwambiri. Ndimo Yesu nadza natosa awo
8 nati, Dzukani, ndimo musaopa. Ndimo kuyang'anayang'ana,
naona palibe modzi, koma Yesu eka.
9 Ndimo monga analikutsika ku piri, Yesu nauza awa, kuti,
Uzani tshoona palibe muntu, kwa ntawi Mwana wa muntu
10 adzaukitsidwa kwa akufa. Ndimo akupunzira atshi
namfunsa, kuti, Ndimo bwanje akulembera anena kuti Eliya
11 akanadza patsogolo? Ndimo naiang'ka nanena, Eliya nditu
12 adza, ndimo adzafotokoza zintu zonse: koma dinena ndi inu,
kuti Eliya anadza kali, ndimo sanamdziwa, koma anatshita
kwa ie zomwe anafuna. Inde tshointsho Mwana wa muntu
13 unso adzamva ndi awo. Ndimo akupunzira nadziwitsa kuti
nanena ndi awo ndi Yohane Mbapatizi.
14 Ndimo ntawi nafika ku antu ambiri, kunadza kwa ie
15 muntu, kugwada kwa ie, ndi kuti, Mwini, kala ndi nsisi ndi
mwana wanga: kuti ali watshizumbazumba, ndimo amva
kwambiri: kuti ntawi zambiri agwa pa moto, ndimo ntawi
16 zambiri m' madzi. Ndimo dinamtenga ku akupunzira ako,
17 ndimo osadziwa kumtshiritsa. Ndimo Yesu naiang'ka nati,
O fuko losamvana ndi kusasamala, ntawi zingati didzakala
ndi inu? ntawi zingati didzalekereza inu? tengani ie kuno
18 kwa ine. Ndimo Yesu nasulumula ie; ndimo demon natu-
ruka kwa ie: ndimo nyamata anatshiritsidwa kwa ora
19 limeneli. Ndimo akupunzira nadza kwa Yesu eka, nanena,
20 Bwanje sitinadziwa ku turutsa ie? Ndimo anena nao,
Tshifuka tsha mvanu woung'ono wanu: kuti dinena ndi
inu nditu, Ngati mupotshera mvanu monga mpetshe ya
mostade, mudzanena ndi piri limene, Sunta apa ku malo a
uko; ndimo lidzasunta; ndimo palibe kantu kadzakala
kosateka kwa inu.
22 Ndimo ntawi nakala m' Galileya, Yesu nanena nao, Mwana

wa muntu adzaperekedwa ku manja a antu; ndimo adzampa, 23
ndi siku latshitatu adzaukitsidwa. Ndimo anali ndi tshisoni
tshambiri.

Ndimo ntawi nafika ku Kapernahum, omwe analandira 24
didrakim nadza kwa Petros, nati, Kodi mpunzitsi wanu
wosalipira didrakim? Ati, Inde. Ndimo ntawi naloa m' 25
nyumba, Yesu nanena patsogolo ndi ie, kuti, Uganiza tshiani,
Simon? mafumu otshuka a dziko, alandira kulipira kapena
tsong'ko kwa ani? kwa ana ao, kapena kwa olendo? Ndimo 26
ntawi nanena, Kwa olendo, Yesu nanena nai', Ndimo ana ali
aufulu. Koma, kani tikwiitsa awo, muka ku nyanja, nu- 27
ponya mbedza, nutenga nsomba yomwe ituruka poiamba;
ndimo ntawi watsegula nkamwa mwatshi, udzapeza shekele:
tenga limene, nupatsa kwa awo kwa ine ndi iwe.

Mwa ora limene akupunzira anadza kwa Yesu, kuti, 18
Ndimo ndani ali wang'kuru wopambana m' dziko la
kumwamba? Ndimo naitana kwa ie kamwana, nakaika 2
pakati pa awo, nati, Dinena ndi inu nditu, Kani 3
mutembenuka, ndimo mukala monga tiana, simudzaloa
nditu m' dziko la kumwamba. Ndimo emwe adzitshepetsa 4
monga kamwana kamene, emwe ali wang'kuru wopambana
m' dziko la kumwamba. Ndimo emwe adzalandira kamwana 5
kamodzi kotere m' dzina langa alandira ine: koma emwe 6
adzakwiitsa kamodzi kwa tiana timene tomwe timvana
ndi ine, tshiri tshopindulidwa kwa ie kuti mpero yeikuru
ya mwala ikamangiridwa pa nkosi patshi, ndi *kuti*
akabizidwa m' kuya kwa nyanja. Tshaipa kwa dziko 7
tshifuka tsha makwiitso! kuti kukanali kuti makwiitso
adza; koma tshaipa kwa muntu uyu mwa emwe kwiitso
lidza! Ndimo ngati dzanja lako kapena pazi lako 8
zikutshimwitsa, dula izo, nuzitaia kwa iwe; tshiri
tshabwino kwa iwe ku loa m' moyo watshipunumbu tsha
nkono kapena wopunduka muendo, kopambana kupotshera
manja awiri kapena mapazi awiri ku ponyedwa m' moto
wosamariza. Ndimo ngati diso lako likutshimwitsa, 9
ulikolole, nulitaia kwa iwe: tshiri tshabwino kwa iwe ku
loa m' moyo ndi diso limodzi, kopambana kupotshera maso
awiri ku ponyedwa m' geena wa moto. Yang'anirani kuti 10
musalalatila kamodzi kwa tiana timene; kuti dinena ndi
inu, kuti m' mwamba anjelo ao ntawi zonse ayang'ana
nkope ya Atatu anga emwe ali m' mwamba. Muganiza 12
bwanje? ngati muntu modzi ali ndi nkosa makumi okaoka

kumi, ndi imodzi ya izo inasotshera, kodi wosazisia makumi
asanu ndi anai, ndi zisanu ndi zinai, nang'ka m' mapiri,
13 nafuna yomwe isotshera? Ndimo ngati kungokala aipeza,
dinena ndi inu nditu, asekera pa iyo kopambana pa
makumi asanu ndi anai, ndi zisanu ndi zinai zomwe
14 zisanasotshera. Inde tshointshi sikuli kufuna kwa Atatu
anu emwe ali m' mwamba, kuti kamodzi kwa tiana timene
tikamwazika.
15 Ndimo ngati mbali wako atshimwa pa iwe, ing'ka,
nusonya ie tshimo latshi inu noka, ngati amva iwe,
16 unapindula mbali wako. Koma ngati wosamva *iwe*, tenga
ndi iwe modzi kapena awiri opambana, monga kuti m'
nkamwa mwa omariza awiri kapena atatu mau onse
17 angolimbikitswa. Ndimo ngati akana ku mva awa, uza
eklesia: ndimo ngati akana ku mva eklesia anso, akale ndi iwe
18 monga muntu wa Mitundu, ndi wolandira tsong'ko. Dinena
ndi inu nditu, Zintu zomwe mudzamanga pansi pano
zidzamangidwa m' mwamba: ndi zintu zomwe mudzamasula
19 pansi pano zidzamasulidwa m' mwamba. Dinena anso ndi
inu, kuti ngati awiri a inu adzaanjana pansi pano ndi kantu
kuti adzafunsa, kadzatshitidwa kwa awo ndi Atatu anga
20 emwe ali m' mwamba. Kuti pomwe awiri kapena atatu
asong'kanitswa m' dzina langa, apo diri pakati pa awo.
21 Pomwe Petros nadza, nanena nai', Mwini, mbali wanga
adzatshimwa kangati pa ine, ndimo didzamkululukira?
22 kwa ntawi zisanu ndi ziwiri? Yesu anena nai', Sindinena
ndi iwe, Kwa ntawi zisanu ndi ziwiri; koma, Kwa ntawi
23 makumi asanu ndi awiri, okaoka zisanu ndi ziwiri. Ndimo
dziko la kumwamba lifanizidwa ndi fumu yotshuka, yomwe
24 inafuna ku wereng'jera ndi akapolo atshi. Ndimo ntawi
anaamba ku wereng'jera, modzi anatengedwa kwa ie, emwe
25 nakong'gola ie matalente mazousan kumi. Koma tshifuka
ali wopanda *kantu* ku bwezera, mwini watshi namuza ku
gulitsidwa, ndi nkazi watshi, ndi ana, ndi zonse zomwe anali
26 nazo, ndi kubweza ku pangidwa. Ndimo kapolo nagwa
napembedza ie, kuti, Mwini, potshera kulongosola ndi ine,
27 ndidzabwezera iwe zonse. Ndimo mwini wa kapolo amene,
anamva tshisoni, nammasula, nakululukira ie gong'gole.
28 Koma kapolo ameneyo naturuka, napeza modzi wa akapolo
anzatshi, emwe nakong'gola ie madenariyon makumi okaoka
kumi: namtenga, na*m*gwira pa kosi, kuti, Bweza tshomwe
29 utshikong'gola. Ndimo kapolo nzatshi nagwa nampempa,

kuti, Potshera kulongosola ndi ine, ndimo didzakubwezera.
Ndimo sanafuna: koma nang'ka namika m' nyumba ya 30
ndima, kwa ntawi akabweza tshomwe tshinakong'goledwa.
Ndimo ntawi akapolo anzatshi naona tshomwe tshinatshitidwa, 31
anamva tshisoni tshambiri, nadza nanena ndi mwini ao zonse
zomwe zinatshitidwa. Ndimo mwini watshi anamwitana 32
kwa ie, ndimo anena nai', Kapolo woipa, dakulululukira iwe
kong'gole yonse imene, tshifuka kuti unandipempa: kodi 33
iwe enso sinukamva tshisoni ndi kapolo nzako, inde monga
damva tshisoni ndi iwe? Ndimo mwini watshi anakwiira, 34
nampereka kwa ambano kwa ntawi akabwezera zonse zomwe
zinakong'goledwa. Tshointshi inso Atatu anga waku- 35
mwamba adzatshita kwa inu, ngati musakulululukira onse
abali ao kwa mitima yanu.

Ndimo kunali ntawi Yesu anata mau amene, natshoka 19
kwa Galileya nafika ku miraga ya Yudeya patsidia lina la
Yordan; ndimo antu ambiri namtsata; natshiritsa awo apo. 2

Ndimo nadza kwa ie Afarisi, kumyesa, ndimo kuti, Kodi 3
tshiri tshamau *kwa muntu* ku tshotsa nkazi watshi kwa
zifukwa zonse? Ndimo naiang'ka nanena, Kodi simu- 4
nawerenga, kuti iemwe anapanga *awo* kwa kwiamba napanga
awa wamamuna ndi wankazi, nati, Kwa tshifukwa tshimene 5
mamuna adzasia atatu atshi ndi amai atshi, nadzigwirizana
ndi nkazi watshi; ndimo awiri adzakala nyama imodzi?
Monga kuti siali awiri inso, koma nyama imodzi. Ndimo 6
tshomwe Mulungu anamangiriza, palibe muntu amasule.
Anena nai', Ndimo bwanje Moses nauza ku patsa lemba la 7
kulekana, ndi ku*m*tshotsa? Anena nao, Moses tshifuka 8
tsha kulimbika kwanu kwa mitima naleka inu ku tshotsa
akazi anu: koma kwa kwiamba sikunali tshointsho. Ndimo 9
dinena ndi inu, Emwe adzatshotsa nkazi watshi, koma kwa
dama, ndimo adzakwata wina, atshita tshigololo: ndi emwe
akwata ie ntawi atshotsedwa atshita tshigololo. Akupunzira 10
anena nai', Ngati mlandu wa mamuna uli tshointsho ndi
nkazi watshi, sitshiri tshabwino ku kwata. Koma nanena 11
nao, Antu onse osadziwa ku landira mau amene, koma
awo kwa omwe apatsidwa. Kuti iripo mifule, yomwe 12
inabadwa tshointsho kwa tshibaliro tsha amai ao: ndimo
iripo mifule, yomwe inapangidwa mifule ndi antu: ndimo
iripo mifule, yomwe inadzipanga mifule kwa dziko la
kumwamba. Iemwe ali ndi mpamvu ku landira, alandire.

Ndimo kunatengedwa kwa ie tiana tating'ono, monga 13

kuti akaika manja atshi pa ito, ndimo akapempera: ndimo
14 akupunzira nasulumula ito. Koma Yesu nati, Lekani tiana
tating'ono, ndimo musatiletsa, ku dza kwa ine: kuti kwa
15 totere liri dziko la kumwamba. Ndimo naika manja atshi
pa ito, namuka uko.
16 Ndimo ona, modzi nadza kwa ie nanena, Mpunzitsi,
tshintu tshabwino tshiani didzatshitshita, monga kuti
17 didzapotshera moyo wosamariza? Ndimo nanena nai',
Bwanje ufunsa ine ndi tshomwe tshiri tshabwino? Modzi
alipo emwe ali wabwino: koma ngati ufuna ku loa m' moyo,
18 sunga mau. Anena nai', Ati? Ndimo Yesu nati, Usapa,
19 Usatshita tshigololo, Usaba, Usasinjirira, Lemekeza atatu ako
ndi amai ako: ndi, Konda woiandikila wako monga ndi iwe
20 eka. Nyamata anena nai', Zintu zonse zimenezi dinasunga:
21 diri wopanda tshiani kosuntira? Yesu nanena nai', Ngati
ufuna ku kala wakuta, muka, gulitsa tshomwe uli natsho,
nupatsa kwa osauka, ndimo udzali ndi kulemera m'
22 mwamba: ndimo udze, unditsate. Koma ntawi nyamata
anamva mau, namuka ndi tshisoni: kuti anali modzi emwe
anali ndi zintu zazikuru.
23 Ndimo Yesu nanena ndi akupunzira atshi, Dinena ndi inu
nditu, Kuli kolimba kwa muntu wolemera ku loa m' dziko
24 la kumwamba. Ndimo dinena ndi inu unso, Tshiri
tshopepuka kwa gamila ku pisa mpanda ya kasingano, ndi
25 kwa muntu wolemera ku loa m' dziko la Mulungu. Ndimo
ntawi akupunzira anamva, nazizwa kwambiri, kuti, Ndimo
26 ndani adziwa ku pulumutsidwa? Ndimo Yesu kuyang'ana
*awo* nanena nao, Ndi antu tshimene tshosateka; koma ndi
27 Mulungu zintu zonse ziteka. Ndimo Petros naiang'ka
nanena nai', Ona, tasia zonse, tinakutsata; ndimo tilandira
28 tshiani? Ndimo Yesu nanena nao, Dinena ndi inu nditu,
kuti inu nomwe munanditsata, mwa kubadwa kawiri ntawi
Mwana wa muntu adzakala pa mpando wotshuka wa
kupambana kwatshi, inu unso mudzakala pa mipando
yotshuka kumi ndi iwiri, kuweruza mafuko kumi ndi awiri a
29 Sirayeli. Ndimo onse omwe anasia zinyumba, kapena abali,
kapena alongo, kapena atate, kapena amai, kapena ana,
kapena minda, kwa dzina langa, adzalandira makumi
30 okaoka kumi, ndimo adzaloa m' moyo wosamariza. Koma
ambiri adzakala apambuiu *omwe ali* apatsogolo; ndi apatsogolo
20 *omwe ali* apambuiu. Kuti dziko la kumwamba liri lofana ndi
muntu emwe ali mwini wa nyumba, emwe anaturuka mamawa

ku gwiritsa ntshito otshita m' munda mwatshi wa mvina.
Ndimo ntawi anapangana ndi otshita kwa denariyon dzua 2
limodzi, natumiza awo ku munda watshi wa mvina. Ndimo 3
naturuka pa ora latshitatu, naona ena kuima opanda ntshito
m' bwalo la maronda; ndimo ku awo nanena, Endani inu 4
unso m' munda wa mvina, ndi tshomwe tshiri tshabwino
didzakupatsani. Ndimo namuka. Anso naturuka pa ora 5
latshisanu ndi tshimodzi, ndi pa ora latshisanu ndi tshinai,
natshita tshimodzimodzi. Ndimo pa *ora* kumi ndi 6
tshimodzi naturuka, napeza ena kuima; ndimo anena nao,
Bwanje muima pano dzua lonse opanda ntshito? Anena 7
nai', Tshifuka kuti palibe muntu anagwiritsa ife. Anena
nao, Endani inu unso m' munda wa mvina. Ndimo ntawi 8
madzulo nadza, mwini wa munda wa mvina anena ndi
ndindo watshi, Itana otshita, nupatsa awa kulipira kwao,
kuiamba ndi apambuiu kwa apatsogolo. Ndimo ntawi 9
anadza omwe *anagwiritsidwa* pa ora kumi ndi tshimodzi,
analandira onse denariyon. Ndimo ntawi oiamba anadza, 10
anaganiza kuti akalandira kopambana; ndi awa anso ana-
landira onse denariyon. Ndimo ntawi analilandira, nadanda- 11
ula pa mwini wa nyumba, kuti, Amene apambuiu anatshita 12
ora limodzi, ndimo unapanga awo ofanafana ndi ife, tomwe
tinamva kulemera kwa dzua ndi kutenta. Koma naiang'ka 13
nanena ndi modzi wa awo, Mbali sinditshita ndi iwe tshimo:
kodi sunapangana ndi ine kwa denariyon? Tenga 14
tshomwe tshiri tshako, numuka; kuli kufuna kwanga ku
patsa ku amene apambuiu, inde monga kwa iwe. Kodi 15
sitshiri tshamau kwa ine ku tshita tshomwe difuna ndi
zanga? kapena kodi diso lako liri loipa, tshifuka kuti diri
wabwino? Tshointshi apambuiu adzakala apatsogolo, ndi 16
apatsogolo apambuiu.

Ndimo monga Yesu analikukwera ku Yerusalem, natenga 17
akupunzira kumi ndi awiri kutseri, ndimo m' njira nanena
nao, Ona, tikwera ku Yerusalem; ndi Mwana wa muntu 18
adzaperekedwa kwa adzukuru akuru ndi kwa akulembera;
ndimo adzamtsutsa kwa imfa, ndimo adzampereka kwa 19
Mitundu ku zunza, ndi ku kwapula, ndi ku patshika:
ndimo siku latshitatu adzaukitswa.

Ndimo nadza kwa ie amai ao a ana amuna a Zebediya 20
ndi ana amuna atshi, kupembedza *ie* ndi kufunsa kantu
kamodzi kwa ie. Ndimo nanena nai', Ufuna tshiani? 21
Anena nai', Uza kuti ana awiri anga amene angokala, modzi

pa dzanja lamanja lako, ndi wina pa dzanja lamanzere lako,
22 m' dziko lako. Koma Yesu naiang'ka nati, Simudziwa
tshomwe mufunsa. Kodi mudziwa ku mwera tshiko
23 tshomwe didzamwera? Anena nai'. Tidziwa. Anena nao,
Tshiko tshanga mudzamwera nditu: koma ku kala pa dzanja
lamanja langa, ndi pa dzanja lamanzere *langa*, si kwanga ku
patsa, koma *kuli ku awo* kwa omwe kunakonzedwa ndi Atatu
24 anga. Ndimo ntawi kumi anamva, anakwia ndi abali *ao* awiri.
25 Koma Yesu naitana awo kwa ie, nati, Mudziwa kuti oweruza
a Mitundu aweruza iyo, ndi akuru ao atshita mpamvu pa
26 iyo. Si tshointsho tshidzakala mwa inu: koma iemwe
afuna ku kala wang'kuru mwa inu adzakala woimirira wanu;
27 ndi iemwe afuna ku kala woiamba mwa inu adzakala kapolo
28 wanu: inde monga Mwana wa muntu sanafika ku imiriridwa,
koma ku imirira, ndi ku patsa moyo watshi dombolo kwa
ambiri.

29 Ndimo monga natshoka kwa Yeriko, antu ambiri ana-
30 mtsata. Ndimo ona, akungu awiri kukala mbali mwa njira,
ntawi anamva kuti Yesu analikupita, napfula, kuti, Mwini,
31 kala ndi nsisi ndi ife, iwe mwana wa Davide. Ndimo
antu ambiri nadzudzula awo, monga kuti akatontola: koma
napfula kopambana, kuti, Mwini, kala ndi nsisi ndi ife, iwe
32 mwana wa Davide. Ndimo Yesu naima, naitana awo, nati,
33 Mufuna tshiani tshomwe dikatshita kwa inu? Anena nai',
34 Mwini, kuti maso atu atsegulidwe. Ndimo Yesu, kunamva
tshisoni, natosa maso ao: ndimo tsopano lino analandira
kuona kwao, namtsata.

21 Ndimo ntawi nayandika ku Yerusalem, nafika ku Bete-
fage, pa piri la Maolive, pomwe Yesu natumiza akupunzira
2 awiri, kunena nao, Endani m' mudzi womwe uli pandunji
pa inu, ndimo tsopano lino mudzapeza buru womangidwa,
ndi mwana wa buru nai': masulani, ndimo tengani kwa ine.
3 Ndimo ngati modzi anena kantu ndi inu, mudzanena, Mwini
ali ndi kufunidwa ndi awo; ndimo tsopano lino adzatumiza
4 awo. Ndimo tshimene tshinali, monga kuti anangodzazidwa
omwe ananenedwa mwa mprofeti, kuti,

5 Muzani mwana wankazi wa Ziyon,
Ona, Fumu Yotshuka yako idza kwa iwe,
Yoanja, ndi kukwera pa buru,
Ndi pa mwana wa buru.

6 Ndimo akupunzira nang'ka, natshita inde monga Yesu ana-
7 sonyeza awa, natenga buru, ndi mwana wa buru, naika pa

awo miinjiro yao; ndimo nakala pa iyo. Ndi unyinji wa 8
antu ambiri nayala miinjiro yao pa njira; ndi ena nadula
matsatsa kwa mitengo, naayala pa njira. Ndi antu ambiri 9
omwe naenda patsogolo pa ie, ndi omwe natsata, napfula,
kuti, Hosana ku mwana wa Davide: Wodala *ali* ie emwe
adza m' dzina la Mwini; Hosana m' kupambanitsa. Ndimo 10
ntawi naloa m' Yerusalem, mzinda wonse unakantshiridwa,
kuti, Amene ali ani? Ndimo antu ambiri nati, Amene ali 11
mprofeti, Yesu, kwa Nazarete wa Galileya.

Ndimo Yesu naloa m' tempile la Mulungu, naturutsa onse 12
awa omwe nagulitsa nagula m' tempile, natembenuza
magome a akusintana ndrama, ndi mipando ya omwe na-
gulira njiwa; ndimo anena nao, Alembedwa, Nyumba 13
yanga idzatshedwa nyumba ya kupempera: koma muipanga
panga la olanda. Ndimo akungu ndi opunduka miendo 14
nadza kwa ie m' tempile: ndimo natshiritsa awa. Koma 15
ntawi adzukuru akuru ndi akulembera naona zintu zozizwa
zomwe anazitshita, ndi ana omwe analikupfula m' tempile
ndi kunena, Hosana ku mwana wa Davide; anakwia, nanena
nai', Kodi sumva tshomwe awa alikunena? Ndimo Yesu 16
anena nao, Inde: kodi simunawerenga ntawi ina, Kwa
nkamwa mwa makanda ndi tiana takwiamwa wata kuleme-
keza? Ndimo nasia awo naturuka m' mzinda kwa Betaniya, 17
nakala apo.

Tsopano m' mawa monga nabwera ku mzinda, namva 18
njala. Ndimo kuona nkuyu pa njira, nadza kwa iwo, napeza 19
palibe kantu pa iwo, koma masamba oka; ndimo anena
nawo, Palibe dzobala dzibale pa iwe tsopano kwa ntawi
zonse. Ndimo nsanga nkuyu unapakatika. Ndimo ntawi 20
akupunzira nauona, nazizwa, kuti, Bwanje nkuyu unapaka-
tika nsanga? Ndimo Yesu naiang'ka nanena nao, Dinena ndi 21
inu nditu, Ngati mupotshera mvanu, ndimo musaganizaganiza,
musadzatshita koka tshomwe tshitshitidwa ndi nkuyu,
koma inde ngati mudzanena ndi piri limene, Tshikudwa
ndimo ponyedwa m' nyanja, tshidzatshitidwa. Ndimo zintu 22
zonse, zomwe mudzafunsa m' kupempera, kumvana, mudza-
landira.

Ndimo ntawi naloa m' tempile, adzukuru akuru ndi 23
akuru a antu nadza kwa ie monga analikupunzitsa, nati,
Ndi mpamvu yanje utshita zintu zimenezi? ndimo anapatsa
iwe mpamvu imene ndani? Ndimo Yesu naiang'ka nanena 24
nao, Didzafunsa inu unso funso limodzi, lomwe ngati mudza-

ndiuza, ine enso didzauza inu ndi mpamvu yanje ditshita
25 zintu zimenezi. Mbapatisma la Yohane, linadzera kuti?
kwa kumwamba kapena kwa antu? Ndimo nauzana iwo
oka, kuti, Ngati tidzanena, Kwa kumwamba; adzanena ndi
26 ife, Ndimo bwanje musanamvana ndi ie? Koma ngati tidza-
nena, Kwa antu; tiopa antu ambiri; kuti onse aganiza Yohane
27 monga mprofeti. Ndimo naiang'ka Yesu, nati, Sitidziwa.
Nanena nao onso, Kapena sindiuza inu ndi mpamvu
28 yanje ditshita zintu zimenezi. Koma muganiza bwanje?
Muntu anali ndi ana awiri: ndimo nadza kwa woiamba,
29 nati, Mwana, enda tshita lero m' munda wa mvina. Ndimo
naiang'ka nati, Sindifuna: koma pambuiu natembenuka,
30 nang'ka. Ndimo nadza kwa watshiwiri, nanena modzimodzi.
Ndimo naiang'ka nati, Ine *ding'ka*, fumu: ndimo sanang'ka.
31 Uti wa awiri anatshita kufuna kwa Atatu atshi? Anena,
Woiamba. Yesu anena nao, Dinena ndi inu nditu, kuti
olandira tsong'ko ndi akazi atshigololo aloa m' dziko la
32 Mulungu patsogolo pa inu. Kuti Yohane nadza kwa inu
m' njira ya kudeka, ndimo simunamvana ndi ie: koma
olandira tsong'ko ndi akazi atshigololo anamvana ndi ie:
ndi inu, ntawi munaona, musanatembenuka pambuiu monga
kuti munangomvana ndi ie.
33 Imvani fanizo lina: Kunali muntu emwe anali mwini wa
nyumba, emwe naoka munda wa mvina, naika tshinga
kozungulira iwo, nakumbira tshiwira tsha vinyo mwa iwo,
namanga sanja, naubwereka kwa otshita munda, nang'ka
34 ku dziko lina. Ndimo ntawi nsiku ya dzobala inayandika,
natumiza akapolo atshi ku otshita munda, ku landira dzobala
35 dzatshi. Ndimo otshita munda nagwira akapolo atshi,
36 namenya modzi, napa wina, naponya miala pa wina. Anso,
natumiza akapolo ena ambiri opambana awa apatsogolo:
37 natshita kwa awo modzimodzi. Koma pambuiu natumiza
kwa iwo mwana watshi, kuti, Adzalemekeza mwana wanga.
38 Koma otshita munda, ntawi naona mwana, nauzana, Amene
39 ali woloa; tieni, timpe natitenge kuloa kwatshi. Ndimo
40 namgwira, namturutsa m' munda wa mvina, nampa. Ndimo
ntawi mwini wa munda wa mvina adzafika, adzatshita tshiani
41 kwa otshita munda amenewo? Anena nai', Adzamwaza
koipa antu oipa adya, ndimo adzabwereka munda wa mvina
kwa otshita munda ena omwe adzabwezera ie dzobala m'
42 nsiku za idzo. Yesu anena nao, Kodi simunawerenga ntawi
ina m' malemba,

Mwala womwe omangira naukana,
Umene unapangidwa mutu wa ngondia:
Kumene kunali kwa Mwini,
Ndimo kuli kuzizwa m' maso atu?

Ndimo dinena ndi inu, Dziko la Mulungu lidzatshotsedwa 43
kwa inu, ndimo lidzapatsidwa ku mtundu kuturutsa dzobala
dza limene. Ndimo ie emwe agwa pa mwala umene adza- 44
tsholedwa: koma pa iemwe udzagwa, udzambalalitsa monga
fumbi. Ndimo ntawi adzukuru akuru ndi Afarisi anamva 45
mafanizo atshi, nadziwitsa kuti nanena ndi awa. Ndimo 46
ntawi nafuna ku gwira ie, naopa antu ambiri, tshifuka kuti
naganiza ie ali mprofeti.

Ndimo Yesu naiang'ka nanena nao onso ndi mafanizo, 22
kuti, Dziko la kumwamba lifanizidwa ndi fumu yotshuka, 2
yomwe inapanga kudia kwa kukwatitsa kwa mwana watshi,
natumiza akapolo atshi ku itana awa omwe anaitanidwa kwa 3
kudia kwa kukwatitsa: ndimo sanafuna ku dza. Anso 4
natumiza akapolo ena, kuti, Uzani awo omwe aitanidwa,
Ona, dakonzetsa kudia kwanga: ng'ombe zanga ndi zoonene-
petsedwa zanga zipedwa ndi zintu zonse zata: Idzani kwa
kudia kwa kukwatitsa. Koma anapepuza iko, natshoka, 5
modzi ku munda watshi, wina ku maronda atshi: ndi otsala 6
nagwira akapolo atshi, naapweteketsa, naapa. Koma fumu 7
yotshuka inakwiira; ndimo inatumiza magulu a ankhondo
atshi, ndimo inamwaza ambanda amenewo, ndimo inaotsha
mzinda wao. Ndimo anena ndi akapolo atshi, Kukwatitsa 8
kuli kwata, koma awo omwe anaitanidwa sianali oenera.
Ndimo endani ku zimphambano za njira, ndimo monga 9
ambiri monga mudzapeza, mwitane kwa kudia kwa kukwa-
titsa. Ndimo akapolo amenewo naturuka m' zinjira, 10
nasong'kanitsa onse monga ambiri monga napeza, oipa ndi
abwino: ndimo kukwatitsa kunadzazidwa ndi oonera. Koma 11
ntawi fumu yotshuka inaloa ku ona oonera, inaona apo
muntu emwe sanabvala mwinjiro wakukwatitsa: ndimo 12
anena nai', Mbali, bwanje unaloa muno wosabvala mwinjiro
wakukwatitsa? Ndimo sanalankula kantu. Ndimo fumu 13
yotshuka inanena ndi oimirira, Mangani ie manja ndi mapazi,
ndimo mumponya mudima wakunja; kudzali apo, kulira
misozi ndi kukukuta mano. Kuti ambiri aitanidwa, koma 14
owereng'jeka asang'kidwa.

Ndimo Afarisi nang'ka, nauzana bwanje anangomkola m' 15
kunena *kwatshi*. Ndimo atumiza kwa ie akupunzira ao, 16

ndi Aherodi, kuti, Mpunzitsi, tidziwa kuti uli woona,
nupunzitsa njira ya Mulungu m' nteradi, ndimo usa-
17 samala kwa modzi: kuti usasang'ka nkope ya antu. Ndimo
uza ife, Uganiza bwanje? Kodi tshiri tshamau ku patsa
18 tsong'ko kwa Kesare, kapena iai? Koma Yesu nadziwitsa
mpulupulu yao, nati, Mundiyesa ranje, atshinyengo inu?
19 Sonyeza ine ndrama ya tsong'ko. Ndimo atenga kwa
20 ie denariyon. Ndimo anena nao, Kufaniza kumene ndi
21 lemba ziri za ani? Anena nai', La Kesare. Ndimo anena
nao, Ndimo perekani kwa Kesare zintu zomwe ziri za
Kesare; ndi kwa Mulungu zintu zomwe ziri za Mulungu.
22 Ndimo ntawi anamva, nazizwa, namsia, namuka.
23 Pa dzua limene anadza kwa ie Asadusi, omwe anena kuti
24 palibe kuukirira: nafunsa ie, kuti, Mpunzitsi, Moses anati,
Ngati muntu afa, wopanda ana, mpwatshi adzakwata nkazi
25 watshi, ndimo adzaukiritsa mbeu kwa njiratshi. Ndimo
anali ndi ife abali asanu ndi awiri: ndimo woiamba nakwata
nafa, ndimo anali wopanda mbeu nasia nkazi watshi kwa
26 mpwatshi; ndimo modzimodzi watshiwiri inso, ndi watshitatu,
27 kwa watshisanu ndi tshiwiri. Ndimo pambuiu pa onse
28 nkazi anafa. Ndimo m' kuukirira nkazi wa ani adzakala
29 wa asanu ndi awiri? kuti awo onse anali nai'. Koma Yesu
naiang'ka nanena nao, Musotshera, kusadziwa malemba,
30 kapena mpamvu ya Mulungu. Kuti m' kuukirira kapena
osakwata, kapena osapatsidwa ku kwatibwa, koma akala
31 monga anjelo m' mwamba. Koma ndi kuukirira kwa
akufa, kodi simunawerenga tshomwe tshanenedwa ndi
32 inu ndi Mulungu, kuti, Diri Mulungu wa Abraham,
ndi Mulungu wa Yisake, ndi Mulungu wa Yakobi?
Mulungu wosali *Mulungu* wa akufa, koma wa amoyo.
33 Ndimo ntawi antu ambiri anamva, nazizwa ndi kupunzitsa
kwatshi.
34 Koma Afarisi, ntawi anamva kuti anatontoletsa Asadusi,
35 anadzisong'kana. Ndimo modzi wa awo, nkoswe, namfunsa
36 funso, kuyesa ie, Mpunzitsi, ati ali mau opambana m' mau?
37 Ndimo nanena nai', Udzakonda Mwini Mulungu wako ndi
ntima wako wonse, ndi nzimu wako wonse, ndi muwongo
38 mwako mwonse. Amene ali mau opambana ndi oiamba.
39 Ndimo atshiwiri ofana *ndi awo* ali amene, Udzakonda
40 woiandikila wako monga iwe eka. Pa mau awiri amene
apatshika mau onse, ndi aprofeti.
41 Ndimo ntawi Afarisi anasong'kanidwa, Yesu nafunsa awo

funso, kuti, Muganiza nwanje ndi Kristu? ali mwana wa 42
ani? Anena nai', *Mwana* wa Davide. Anena nao, Ndimo 43
Davide m' nzimu amtsha Mwini, bwanje, kuti,

Mwini nanena ndi Mwini wanga, 44
Kala iwe pa dzanja lamanja langa,
Kwa ntawi diika maliwongo ako pansi pa mapazi ako?

Ndimo ngati Davide amtsha ie Mwini, bwanje ali mwana 45
watshi? Ndimo palibe modzi anadziwa kumwiang'ka liu 46
limodzi, kapena muntu wina kwa dzua limene sanayesa
kumfunsa mafunso ena.

Ndimo Yesu nalankula ndi antu ambiri ndimo ndi 23
akupunzira atshi, kuti, Akulembera ndi Afarisi akala pa 2
mpando wa Moses: ndimo zintu zonse zomwe akuuzani, 3
*zimene* tshitani ndi sungirani: koma musatshita ofana ndi
ntshito zao; kuti anena, ndimo osatshita. Inde, amanga 4
akatundu olemera ndi opweteka ku nyamulidwa, naika awa
pa mapuzi a antu; koma awa oka osafuna ku sunta awa ndi
tshala tshao. Koma ntshito zonse zao atshita ku onedwa 5
ndi antu: kuti napanga bwambi lalikuru la mafulaktere ao,
nakuritsa mitsheu *ya mwinjiro yao*, nakonda malo opambana 6
pa kudia, ndi mipando yeikuru mwa masinagoge, ndi mautso 7
mwa malo a maronda, ndi ku tshedwa ndi antu, Rabi.
Koma musatshedwa Rabi: kuti modzi ali mpunzitsi wanu, 8
ndi inu nonse muli abali. Ndimo musatsha muntu modzi 9
atatu anu pansi pano: kuti modzi ali Atatu anu, emwe ali
m' mwamba. Kapena musatshedwa ambuiye: kuti modzi 10
ali mbuiyanu, Kristu. Koma iemwe ali wang'kuru 11
wopambana mwa inu adzakala woimirira wanu. Ndi 12
emwe adzadzipambanitsa adzatshepetsedwa; ndimo emwe
adzadzitshepetsa adzapambanitsidwa.

Koma tshaipa kwa inu, akulembera ndi Afarisi, 13
atshinyengo! tshifuka mutseka dziko la kumwamba pa
antu: kuti kapena musaloa inu noka, kapena musaleka awo
omwe alikuloa ku loa.

Tshaipa kwa inu, akulembera ndi Afarisi, atshinyengo! 15
kuti muzungulira nyanja ndi ntunda ku panga wopinduka
modzi; ndimo ntawi anakala, mupanga ie kawiri kopambana
inu mwana wa geena.

Tshaipa kwa inu, atsatsogolo akungu, omwe muti, Emwe 16
adzalumbira ndi malo oyera, tshiri tshabe; koma emwe
adzalumbira ndi golide la malo oyera, ali wang'gong'goli.
Mwapusa inu ndi akungu: kuti kodi kuli kopambana, 17

kapena golide, kapena malo oyera omwe anayeretsa golide?
18 Ndi, Emwe adzalumbira ndi katshisi tshiri tshabe; koma
emwe adzalumbira ndi tshaulere tshomwe tshiri pa ie,
19 ali wang'gong'goli. Akungu inu: kuti kodi kuli kopa-
mbana, tshaulere, kapena katshisi emwe ayeretsa tshaulere?
20 Ndimo emwe alumbira ndi katshisi, alumbira ndi ie, ndimo
21 ndi zintu zonse pa ie. Ndi emwe alumbira ndi malo oyera,
22 alumbira ndi ie, ndi emwe akala momo. Ndi emwe
alumbira ndi mwamba, alumbira ndi mpando wa Mulungu,
ndimo ndi ie emwe akala pa iwo.
23 Tshaipa kwa inu, akulembera ndi Afarisi, atshinyengo!
kuti mulipira mpambu ya minte ndi ya anise ndi kumine,
ndi simunasamala zolemera za mau, kuweruza, ndi nsisi, ndi
mvanu: koma zimenezi mukanatshita ndi sikusasamala zina.
24 Atsatsogolo akungu inu, omwe mukunta ndi tshifukufuku,
ndi mumwetsa gamila.
25 Tshaipa kwa inu, akulembera ndi Afarisi, atshinyengo!
kuti mutsuka kunja kwa tshiko ndi kwa mbale, koma
26 mbwalo zidzazidwa kwa kulanda ndi kudzilekereza. Mfarisi
wakungu iwe, tsuka patsogolo mbwalo mwa tshiko ndi
mwa mbale, monga kuti kunja kwa izo kungokala
kwatsukidwa anso.
27 Tshaipa kwa inu, akulembera ndi Afarisi, atshinyengo!
kuti muli ofana ndi mianda yopakidwa yovera, yomwe
isonyeza yabwino kunja, koma m' bwalo idzazidwa ndi
28 mafupa a antu akufa, ndi zonse zosatsuka. Inde tshointsho
inu unso kunja musonyeza odeka kwa antu, koma m' bwalo
mudzaza ndi tshinyengo ndi mpulupulu.
29 Tshaipa kwa inu, akulembera ndi Afarisi, atshinyengo!
kuti mumanga mianda ya aprofeti, ndimo mukonzetsa
30 mianda ya odeka, ndimo muti, Ngati tinali m' masiku a
Atatu atu, sitinganakala ogawana ndi awo m' mwazi wa
31 aprofeti. Ndimo kuti mumariza kwa inu noka, kuti muli
32 ana a awa omwe anapa aprofeti. Ndimo dzazani muyezo wa
33 atatu anu. Zinjoka inu, inu fuko la zimpiri, bwanje mudza-
34 dziwa ku pulumuka kusutsa kwa geena? Ndimo, ona,
ditumiza kwa inu aprofeti, ndi antu anzeru, ndi akulembera:
ena a awa mudzapa ndi mudzapatshika; ndi ena a awa
mudzakwapula m' masinagoge anu, ndi mudzatshita nkarwe
35 kwa mzinda ndi mzinda: monga kuti pa inu ingodza miazi
yodeka yonse inaturutsidwa pa dziko, kwa mwazi wa Abeli
wodeka kwa mwazi wa Zekariya mwana wa Berakiya, emwe

munapa pakati pa malo oyera ndi katshisi. Dinena ndi inu 36
nditu, Zintu zonse zimenezi zidzadza pa fuko limene.
O Yerusalem, Yerusalem, womwe upa aprofeti, nu- 37
ponya miala pa awo omwe atumidwa kwa iwo! ntawi zi-
ngati dafuna ku song'kanitsa ana ako, inde monga tadzi
lisong'kanitsa anapie atshi pansi pa mapiko atshi, koma
simunafuna! Ona, nyumba yanu isiidwa kwa inu yadzinja. 38
Kuti dinena ndi inu, Musandiona kwa ntawi yatsopano, 39
kwa ntawi mudzanena, Wodala *ali* iemwe adza m' dzina
la Mwini.

Ndimo Yesu anaturuka kwa tempile, ndimo analikupita; 24
ndimo akupunzira atshi nadza kwa ie ku sonyeza ie
mamangidwe a tempile. Koma naiang'ka nanena nao, Kodi 2
simuona zintu zonse zimenezi? dinena ndi inu nditu,
Wosadzasiidwa pano mwala umodzi pa wina, womwe wosadza-
ponyedwa.

Ndimo monga nakala pa piri la Maolive, akupunzira 3
nadza kwa ie kutseri, kuti, Utiuze, zintu zimenezi zidzakala
liti? ndi tshiani *tshidzakala* tshizindikilo tsha kudza
kwako, ndi tshakumariza kwa kugonera? Ndimo Yesu 4
naiang'ka nanena nao, Tshenjerani kuti palibe muntu
akusotsherezani. Kuti ambiri adzadza m' dzina langa, kuti, 5
Diri Kristu, ndimo adzasotshereza ambiri. Ndimo 6
mudzamva ndi zinkondo ndi mbiri za zinkondo: yang'anirani
kuti musantuntumiridwa: kuti *zintu zimenezi* zikanakala;
koma nsonga siiri kosuntira. Kuti mtundu udzauka pa 7
mtundu, ndi dziko pa dziko: ndimo kudzali zaola ndi
zibvomezi m' malo ena. Koma zintu zonse zimenezi ziri 8
zoiamba za tshisoni. Pomwe adzapereka inu kwa sautso, 9
ndimo adzapa inu: ndimo mudzakwiitsidwa ndi mitundu
yonse kwa dzina langa. Ndimo pomwe ambiri adzakwii- 10
tsidwa, ndimo adzaperekana, ndimo adzakwiirana. Ndimo 11
aprofeti ambiri onyenga adzauka, ndimo adzasotshereza
ambiri. Ndimo tshifuka mpulupulu idzapindulidwa, 12
kukonda kwa ambiri kudzakala kwazizira. Koma iemwe 13
akalabe kwa kumariza, iemwe adzapulumutsidwa. Ndimo 14
ivangeli umene wa dziko udzauzidwa mwa dziko lonse kwa
lomariza ku mitundu yonse; ndimo pomwe kumariza
kudzadza.

Ndimo ntawi muona kunyansa kwa dzinja, komwe 15
kwanenedwa mwa Danyeli mprofeti, kuima m' malo oyera
(iemwe awerenga adziwe), pomwe omwe akala m' Yudeya 16

17 atawire ku mapiri: emwe ali pamwamba pa nyumba asatsike
18 ku tenga zintu zomwe ziri m' nyumba yatshi: ndimo emwe
ali m' munda asabwerere ku tenga tshopfunda tshatshi.
19 Koma tshaipa kwa awo omwe ali ndi mimba ndi kwa awo
20 omwe ayamwitsa m' masiku awo! Ndimo pemperani kuti
kutawa kwanu sikudzali m' malimwe, kapena pa sabata:
21 kuti pa ntawi imene kudzali sautso yeikuru, yotere monga
siinali kwa kwiamba kwa dziko kwa tsopano, iai, kapena
22 siidzali ntawi ina. Ndimo kani masiku amenewo
anafupitsidwa, palibe nyama inakapulumutsidwa: koma
23 kwa osang'kidwa masiku amenewo adzafupitsidwa. Ndimo
ngati muntu modzi adzati kwa inu, Ona, Kristu ali pano,
24 kapena, Apa; musamvana. Kuti adzauka Akristu anyenga,
ndi aprofeti anyenga, ndimo adzasonyeza zizindikilo zazi-
kuru ndi zozizwa; monga kuti ku sotshereza, ngati
25 kuli kuteka, inde osang'kidwa. Ona, dauza inu patsogolo.
26 Ndimo ngati adzanena ndi inu, Ona, ali m' tshipululu;
musaturuka: Ona, ali m' dzipinda dzambwalo; musamvana.
27 Kuti monga mpezi ituruka ku bvuma, ndimo ionedwa
inde ku zambwe; tshointshi kudzakala kudza kwa
28 Mwana wa muntu. Pomwe ntembo ulipo, apo miimba
idzasong'kanidwa.
29 Koma tsopano lino, pambuiu pa sautso ya masiku awo,
dzua lidzadetsedwa, ndi mwezi sudzapatsa kuunika kwatshi,
ndi nyenyezi zidzagwa kwa kumwamba, ndi mpamvu za
30 miamba zidzantuntumiritsidwa: ndimo pomwe tshidzaone-
tswa tshizindikilo tsha Mwana wa muntu m' mwamba:
ndimo pomwe mitundu yonse ya pansi idzakala ndi tshisoni,
ndimo idzaona Mwana wa muntu kudza m' mitambo ya
31 mwamba ndi mpamvu ndi kupambana kwakukuru. Ndimo
adzatumiza anjelo atshi ndi namalowe wang'kuru wa lipenga,
ndimo adzasong'ketsa osang'kidwa atshi kwa mpepo zinai,
kwa nsonga imodzi ya kumwamba kwa ina.
32 Ndimo kwa nkuyu punzirani fanizo latshi: ntawi tsatsa
latshi likala lotepa, naliturutsa masamba atshi, mudziwa kuti
33 dzinja liri pafupi; inde tshointshi inu unso, ntawi muona
zintu zonse zimenezi, dziwani kuti ali pafupi, *inde* pa
34 dzitseko. Dinena ndi inu nditu, Fuko limene losadzapita,
35 ku ntawi zintu zonse zimenezi zidzatedwa. Kumwamba ndi
36 dziko zidzapita, koma mau anga sadzapita. Koma ndi
siku limene ndi ora palibe modzi adziwa, iai, si inde anjelo
37 a kumwamba, kapena Mwana, koma Atate eka. Ndimo

monga masiku a Nowa, tshointshi kudzakala kudza kwa
Mwana wa muntu. Kuti monga m' masiku awo omwe anali 38
patsogolo pa tshigumula analikudia ndi kumwa, kukwata
ndi kupatsa ku kwatibwa, kwa siku lomwe Nowa naloa m'
tshombo, ndimo sanadziwa kwa ntawi tshigumula tshinadza, 39
natshotsa awo onse; tshointshi kudzakala kudza kwa
Mwana wa muntu. Pomwe adzali antu awiri m' munda; 40
modzi atengedwa, ndi modzi asiidwa: akazi awiri *adza-* 41
*li*kupera pa mpero; modzi atengedwa, ndi modzi asiidwa.
Ndimo dikirani: kuti simudziwa siku liti Mwini wanu 42
adza. Koma dziwani tshimenetshi, kuti ngati mwini wa 43
nyumba anadziwa m' kudikira kuti woba analinkudza,
akanadikira ndimo akanaletsa nyumba yatshi ku boledwa.
Ndimo mwata inu unso: kuti m' ora lomwe simuganiza, 44
Mwana wa muntu adza. Ndimo ndani ali kapolo wamvanu 45
ndi wotshenjera, emwe mwini watshi anaika pa banja latshi,
ku patsa kudia kwao pa ntawi yabwino? Wodala ali kapolo 46
amene, emwe mwini watshi ntawi adza adzapeza alikutshita
tshointsho. Dinena ndi inu nditu, kuti adzaika ie pa zonse 47
zomwe ali nazo. Koma ngati kapolo woipa amene adzanena 48
muntima mwatshi, Mwini wanga atshedwa; ndimo 49
adzaamba ku menya akapolo anzatshi, ndimo adzadia ndi
ku mwa ndi oledzera; mwini wa kapolo amene adzadza m' 50
siku ntawi wosayang'anira, ndi m' ora ntawi wosadziwa,
ndimo adzadula ie, nadzasonyeza pande latshi ndi atshi- 51
nyengo: pomwe kudzali kulira ndi kukukuta mano.

Pomwe dziko la kumwamba lidzafanizidwa ndi dziweta 25
kumi, dzomwe dzinatenga nyali zao, dzinaturuka ku komana
ndi wokwati. Ndimo dzisanu dza idzo dzinali dzopusa, 2
ndimo dzisanu dzinali dzotshenjera. Kuti dzopusa, ntawi 3
dzinatenga nyali zao, dzinatenga palibe mafuta ndi idzo:
koma dzotshenjera dzinatenga mafuta m' dziwira dzao ndi 4
nyali zao. Ndimo ntawi wokwati natshedwa, dzonse dzina- 5
sinza, dzinagona tulo. Koma pakati pa usiku kuli kupfula, 6
Ona, wokwati! Turukani ku komana nai'. Ndimo dziweta 7
dzonse idzo dzinauka, dzinafotokoza nyali zao. Ndimo 8
dzopusa dzinanena ndi dzotshenjera, Tipatseni mafuta
anu; kuti nyali zatu zirikuzima. Koma dzotshenjera dzi- 9
naiang'ka, kuti, Kani sadzakwana kwa ife ndi inu: mukani
kopambana kwa awo omwe agulitsa, ndimo mugula kwa inu
noka. Ndimo ntawi dzinang'ka ku gula, wokwati nafika; 10
ndi dzomwe dzinata dzinaloa ndi ie kwa kudia kwa kukwa-

11 titsa: ndimo tshitseko tshinatsekedwa. Pambuiu dzidza
12 anso dziweta dzina, kuti, Mwini, Mwini, tsegulira ife. Koma
naiang'ka nati, Dinena ndi inu nditu, Sindidziwa inu.
13 Ndimo dikirani, kuti musadziwa kapena siku kapena ora.
14 Kuti *kuli* monga *ntawi* muntu, kuenda m' dziko lina,
naitana akapolo atshi, napereka kwa awo zintu zatshi.
15 Ndimo ku modzi anapatsa matalente asanu, ku wina awiri,
ku wina limodzi; ku onse monga mpamvu zao; ndimo
16 namuka. Tsopano lino iemwe analandira matalente asanu
nang'ka natsatsa ndi amenewa, napindula ena matalente
17 asanu. Tshointsho ie enso emwe *analandira* awiri napindula
18 awiri ena. Koma iemwe analandira limodzi nang'ka nakumba
19 pansi, nabisa ndrama ya mwini watshi. Ndimo pambuiu pa
ntawi yeitali mwini wa akapolo amenewo adza, nawereng'-
20 jera nao. Ndimo emwe analandira matalente asanu nafika
natenga matalente ena asanu, kuti, Mwini, unapatsa ine
matalente asanu: ona, dapindula matalente ena asanu.
21 Mwini watshi nanena nai', Tshakoma, kapolo wabwino ndi
wamvanu: wakala ndi mvanu pa zintu zowereng'jeka,
didzaika iwe pa zintu zambiri: loa iwe m' tshimwemwe
22 tsha mwini wako. Ndimo ie enso emwe *analandira* mata-
lente awiri nadza nati, Mwini, unapatsa ine matalente awiri:
23 ona, dapindula matalente ena awiri. Mwini watshi nanena
nai', Tshakoma, kapolo wabwino ndi wamvanu; wakala ndi
mvanu pa zintu zowereng'jeka, didzaika iwe pa zintu
24 zambiri: loa iwe m' tshimwemwe tsha mwini wako. Ndimo
ie enso emwe analandira talente limodzi nadza nati, Mwini,
dinadziwa iwe kuti uli muntu wouma, kutema pomwe
25 usanafesa, ndi kukung'ka pomwe usanataia: ndimo dinaopa,
dinang'ka ndinabisa talente lako pansi: ona, uli ndi lako.
26 Koma mwini watshi naiang'ka nanena nai', Kapolo iwe
woipa ndi wolesi, unadziwa kuti ditema pomwe sindinafesa,
27 ndimo dikung'ka pomwe sindinataia; ndimo ukanaikirira
ndrama zanga ku osinta, ndimo pa kudza kwanga dikana-
28 landira zanga ndi kupindula. Ndimo tshotsani talente kwa
ie, ndimo patsani ilo kwa emwe anali ndi matalente kumi.
29 Kuti kwa onse omwe apotshera adzapatsidwa, ndimo adzapo-
tshera zambiri: koma kwa emwe wosapotshera, inde zomwe
30 ali nazo zidzatshotsedwa. Ndimo ponyani kapolo wosapi-
ndula mudima wakunja: apo kudzali kulira nsozi ndi kuku-
kuta mano.

31 Koma ntawi Mwana wa muntu adzadza m' kupambana

kwatshi, ndi anjelo onse nai', pomwe adzakala pa mpando
wotshuka wa kupambana kwatshi: ndimo patsogolo pa ie 32
idzasong'kanitswa mitundu yonse: ndimo adzasang'ka iwo
umodzi kwa wina, monga mbusa asang'ka nkosa kwa agogo:
ndimo adzaika nkosa pa dzanja latshi lamanja, koma agogo 33
pa lamanzere. Ndimo Fumu Yotshuka idzanena nao pa 34
dzanja latshi lamanja, Idzani, odala inu a Atatu anga, loani
m' dziko lafotokozedwa kwa inu kwa kuzika kwa dziko:
kuti dinamva njala, ndimo munapatsa ine kudia: dinamva 35
ludzu, ndimo munapatsa ine kumwa: dinali mlendo, ndimo
munandiloetsa; wamariseke, ndimo munandibveka: dina- 36
dwala, ndimo munanditshezetsa: dinali m' nyumba ya ndima,
ndimo munadza kwa ine. Ndimo odeka adzaiang'ka ie, kuti, 37
Mwini, tinaona iwe ndi njala liti, ntinaweta iwe? kapena
ndi ludzu, ntinakumwetsa? Ndimo tinakuona mlendo liti, 38
ntinakuloetsa? kapena wamariseke, ntinakubveka? Ndimo 39
tinaona iwe wodwala liti, kapena m' nyumba ya ndima,
ntinadza kwa iwe? Ndimo Fumu Yotshuka idzaiang'ka 40
nidzanena nao, Dinena ndi inu nditu, Mwa kuti munatshi-
tshita ndi modzi wa amene abali anga, *inde* amene ang'ono
opambana, munatshitshita kwa ine. Ndimo idzanena anso 41
ku awa pa dzanja lamanzere, Tshokani kwa ine, inu
olumbiridwa, m' moto wosamariza womwe ufotokozedwa
kwa diabolos ndi anjelo atshi: kuti dinamva njala, ndimo 42
simunandipatsa kudia: dinamva ludzu, ndimo simunandi-
mwetsa: dinali mlendo, ndimo simunandiloeza; wamariseke, 43
ndimo simunandibveka; wodwala, ndi m' nyumba ya
ndima, ndimo simunanditshezetsa. Ndimo adzamwiang'ka 44
anso, kuti, Mwini, tinaona iwe ndi njala liti, kapena
ndi ludzu, kapena mlendo, kapena wamariseke, kapena
wodwala, kapena m' nyumba ya ndima, ndimo sitinaimirira
kwa iwe? Ndimo adzaiang'ka awo, kuti, Dinena ndi inu 45
nditu, Monga ambiri monga simunatshitshita ndi modzi
wa amene ang'ono opambana, simunatshitshita kwa ine.
Ndimo amene adzatshoka kwa kulanga kosamariza: koma 46
odeka kwa moyo wosamariza.

Ndimo kunali, ntawi Yesu anata mau onse amene, nanena 26
ndi akupunzira atshi, Mudziwa kuti pambuiu masiku awiri 2
kuli mpasika, ndimo Mwana wa muntu aperekedwa ku
patshikidwa. Ndimo anasong'kanitswa adzukuru akuru, ndi 3
akuru a antu, ku bwalo kwa ndzukuru wang'kuru, emwe
anatshedwa Kayafa; ndimo nafunsana kuti anangogwira 4

5 Yesu ndi tshinyengo, nangompa. Koma nati, Si pa *siku la*
kudia, kani pokoso likala mwa antu.
6 Ndimo ntawi Yesu anali m' Betaniya, m' nyumba ya
7 Simon wakate, nadza kwa ie nkazi anali nayo nsupa ya
alabastile ya mafuta, ntengo watshi wapatali nditu, ndimo
8 naatsanula pa mutu patshi, monga nakala pa kudia. Koma
ntawi akupunzira anaona, nakala ndi kukwia, kuti, Kwa
9 tshiani kuli kusakaza kumene? Kuti *mafuta* amenewa
anangogulitsidwa kwa zambiri, napatsidwa kwa osauka.
10 Koma Yesu kudziwitsa nanena nao, Mumvuta bwanje
11 nkazi? kuti anatshita ntshito yabwino pa ine. Kuti
mupotshera osauka ndi inu ntawi zonse; koma ine musapo-
12 tshera ntawi zonse. Kuti mwa amene anatsanula mafuta
amene pa tupi langa, anatshita ku konzetsa ine kwa kuika
13 m' mwanda. Dinena ndi inu nditu, Pa malo omwe ivangeli
umene udzauzidwa mwa dziko lonse, tshimene enso tshomwe
nkazi amene watshita tshidzalankulidwa kwa tshikumbutso
tsha ie.
14 Pomwe modzi wa kumi ndi awiri, emwe anatshedwa Yuda
15 Sikariyoti, nang'ka ku adzukuru akuru, nanena, Mufuna
kundipatsa tshiani, ndimo didzapereka ie kwa inu? Ndimo
16 nayeza kwa ie zipinjiri za silivere makumi atatu. Ndimo
kwa ntawi imene nafuna pofatsa kumpereka *kwa awo.*
17 Ndimo pa *siku* loamba la nkate wopanga tshabe aku-
punzira nadza kwa Yesu, kuti, Pati ufuna kuti tifotokozere
18 kwa iwe ku dia mpasika? Nati, Mukani muzinda ku
muntu modzi, ndimo munena nai', Mpunzitsi ati, Ntawi
yanga iri pafupi; disunga mpasika pa nyumba yako ndi
19 akupunzira anga. Ndimo akupunzira natshita monga Yesu
20 anauza awa; nafotokoza mpasika. Tsopano ntawi madzulo
anadza, analikukala pa kudia ndi akupunzira kumi ndi
21 awiri; ndimo monga analinkudia, nati, Dinena ndi inu nditu,
22 kuti modzi wa inu adzandizonda. Ndimo anali ndi tshisoni
tshambiri nditu, naamba modzi ndi modzi wa onse ku nena
23 nai', Kodi diri ine, Mwini? Ndimo naiang'ka nati, Iemwe
anasunsa dzanja latshi ndi ine m' mbale, emwe adzandizonda.
24 Mwana wa muntu apita, inde monga alembedwa ndi ie:
koma tshaipa ku muntu amene mwa emwe Mwana wa muntu
azondedwa! kunali bwino kwa muntu amene ngati
25 sanabadwa. Ndimo Yuda, emwe anamzonda, naiang'ka
26 nati, Kodi ndine, Rabi? Anena nai', Iwe unati. Ndimo
monga analinkudia, Yesu natenga nkate, nadalitsa, nauswa;

napatsa ku akupunzira, nati, Tengani, idiani; umene uli
tupi langa. Ndimo natenga tshiko, nati tshakoma, napatsa 27
ku awa, kuti, Imwani onse ndi itsho; kuti umene uli 28
mwazi wanga wa testamente, womwe uturutsidwa kwa
ambiri kwa kubweza kwa zakwaipa. Koma dinena ndi 29
inu, Sindidzamwa ntawi ina ndi tshobala tshimene tsha
mvina, kwa siku limenelo lomwe dimwa itsho tshatsopano
ndi inu m' dziko la Atatu anga.

Ndimo ntawi anaimba nyimbo, naturuka ku piri la 30
Maolive.

Pomwe Yesu anena nao, Inu nonse mudzakwiitsidwa 31
mwa ine usiku uno: kuti alembedwa, Didzakoma mbusa, ndi
nkosa za gulu zidzabalalitsidwa. Koma pambuiu diukitswa, 32
didzaenda patsogolo pa inu m' Galileya. Koma Petros 33
naiang'ka nanena nai', Ngati onse adzakwiitsidwa mwa iwe,
ine sindidzakwiitsidwa ntawi ina. Yesu nanena nai', 34
Dinena ndi iwe nditu, kuti usiku uno, patsogolo tambala
alira, udzandikana katatu. Petros anena nai', Inde ngati 35
dikanafa ndi iwe, *kosuntira* sindidzakukana. Tshointsho
onso nanena akupunzira onse.

Ndimo Yesu adza ndi awa ku malo atshedwa Getsemane, 36
ndimo anena ndi akupunzira atshi, Kalani pano, ntawi
dipita uko ku pempera. Ndimo natenga nai', Petros ndi ana 37
amamuna awiri a Zebediya, ndimo naamba ku kala ndi
tshisoni ndi ku sautsidwa kwambiri. Ndimo anena nao, 38
Nzimu wanga uli ndi tshisoni tshambiri, inde kwa imfa:
kalani pano, ndimo dikirani ndi ine. Ndimo naenda 39
patsogolo pang'ono, nagwa pa nkope yatshi, napempera,
kuti, O Atatu anga, ngati kuli kuteka, leka tshiko tshimene
ku tshoka kwa ine: koma, si monga difuna, koma monga
u*funa*. Ndimo adza ku akupunzira, ndimo aapeza alikugona, 40
nanena ndi Petros, Nanga bwanje, musadziwa ku dikira ndi
ine ora limodzi? Dikirani ndimo pemperani, kuti musaloa 41
m' tshinyengo: nzimu uli wakufuna nditu, koma nyama
ilefuka. Anso, ntawi yatshiwiri nang'ka, napempera, kuti, 42
O Atatu anga, ngati tshimene sitshingotshoka, kani dimwa
ndi itsho, kufuna kwako kutshitidwe. Nadza anso napeza 43
awa alikugona, kuti maso ao analemera. Ndimo nasia awa 44
anso, nang'ka, napempera ntawi yatshitatu, kuti inso mau
amodzimodzi. Pomwe adza ku akupunzira, ndimo anena 45
nao, Gonani tsopano, ndimo tengani kupuma kwanu: ona,
ora liri pafupi, ndi Mwana wa muntu azondedwa kwa

46 manja a ampulupulu. Dzukani, tidzing'ke: ona, ali pafupi
emwe andizonda.
47 Ndimo ntawi analikulankula, ona, Yuda, modzi wa kumi
ndi awiri, nadza, ndimo ndi ie anali antu ambiri ndi mipeni
ya nkondo ndi zindodo, kwa adzukuru akuru ndi akuru a
48 antu. Ndimo iemwe anamzonda napatsa awa tshizindi-
kilo, kuti, Iemwe didzamsomsona, iemwe ali ie: gwirani
49 ie. Ndimo tsopano lino nadza kwa Yesu, nati, Kala
50 bwino, Rabi; namsomsona. Ndimo Yesu nanena nai',
Mbali, *tshita* tshimene kwa tshomwe wadzera. Pomwe
51 anadza naika manja pa Yesu, namgwira. Ndimo ona,
modzi wa awo omwe anali ndi Yesu naturutsa dzanja latshi,
naturutsa mpeni watshi wa nkondo, nasenga kapolo wa
52 ndzukuru wang'kuru, nadula kutu latshi. Pomwe Yesu
anena nai', Ika anso mpeni wako wa nkondo m' malo atshi:
kuti onse awo omwe atenga mpeni wa nkondo, adzamwazika
53 ndi mpeni wa nkondo. Kapena uganiza kuti sindi-
dziwa ku pempa Atatu anga, ndimo inde tsopano lino
adzanditumizira opambana malijon kumi ndi awiri a anjelo?
54 Ndimo bwanje malemba angodzazidwa, kuti tshointshi
55 akanali? M' ora limene Yesu nanena ndi antu ambiri,
Kodi muturuka monga pa wolanda ndi mipeni ya nkondo
ndi zindodo kundigwira? Dakala masiku onse m' tempile
56 kupunzitsa, ndimo simunagwira ine. Koma onse amene
atshitidwa, kuti malemba a aprofeti angodzazidwa. Pomwe
akupunzira onse namsia, natawa.
57 Ndimo awo omwe anagwira Yesu namtsogoza kwa *nyumba*
*ya* Kayafa ndzukuru wang'kuru, pomwe akulembera ndi
58 akuru anasong'kanidwa. Koma Petros namtsata kutali, kwa
bwalo la ndzukuru wang'kuru, naloa, nakala pansi ndi oimi-
59 rira, ku ona nsonga. Ndimo adzukuru akuru ndi gulu
lonse la ankoswe nafuna kumariza kwakunama pa Yesu,
60 kuti anangompa; ndimo sanakupeza ngati omariza onama
61 ambiri nadza. Koma pambuiu nadza awiri, nati, Muntu
amene nati, Didziwa ku mwaza malo oyera a Mulungu, ndi
62 kuamanga m' masiku atatu. Ndimo ndzukuru wang'kuru
nauka, nanena nai', Suiang'ka kantu? tshiri tshiani tshomwe
63 amene amariza pa iwe? Koma Yesu natontola. Ndimo
ndzukuru wang'kuru nanena nai', Dikulimbika ndi Mulungu
wamoyo, kuti utiuza ngati uli Kristu, Mwana wa Mulungu.
64 Yesu anena nai', Wati: koma dinena ndi inu, Pambuiu
mudzaona Mwana wa muntu kukala pa dzanja lamanja la

mpamvu, ndi kudza pa mitambo ya kumwamba. Pomwe 65
ndzukuru wang'kuru nang'amba nsaru zatshi, kuti, Wanena
kutukwana: kufunidwa kwina kwanje kopambana tipotshera
kwa omariza? ona, tsopano munamva kutukwana: muga- 66
niza bwanje? Naiang'ka nati, waenedwa kwa imfa.
Pomwe nalabvula mate pa nkope patshi nambwandula: ndi 67
ena namkanta ndi dzikatu dza manja ao, kuti Losera ife, 68
Kristu iwe: ndani ali ie emwe anakukanta?

Ndimo Petros analikukala kunja m' bwalo. ndimo butu 69
linadza kwa ie, kuti, Iwe enso unali ndi Yesu Mgalileya.
Koma nakana patsogolo pa onse, kuti, Sindidziwa tshomwe 70
unena. Ndimo ntawi anaturuka ku balanda, lina linamona, 71
ndimo linena nao omwe anali apo, Muntu amene enso anali
ndi Yesu Mnazarete. Ndimo onso nakana ndi lumbiro, 72
Sindidziwa muntu. Ndimo pambuiu ntawi yeing'ono awo 73
omwe anaima pafupi nadza nanena ndi Petros, M' nteradi
uli inso *modzi* wa awo; kuti kulankula kwako kusonyeza
iwe. Pomwe naamba ku tukwana ndi ku lumbira, Sindi- 74
dziwa muntu. Ndimo tsopano lino tambala nalira. Ndimo 75
Petros nakumbukila mau omwe Yesu ananena, Patsogolo
tambala alira, udzandikana katatu. Ndimo naturuka,
nalira kwambiri ndi nsozi.

Ndimo ntawi mamawa anadza, adzukuru akuru onse 27
ndi akuru a antu nafunsana pa Yesu kumpa: ndimo 2
anammanga, namtsogoza, napereka ie ku Pilato
mbiri.

Ndimo Yuda, emwe anamzonda, ntawi naona kuti anasu- 3
tsidwa, natembenuka ie eka, nabweza zipinjiri makumi
atatu za silivere kwa adzukuru akuru ndi akuru, kuti,
Datshimwa mwa tshimenetshi dazonda mwazi wopanda 4
kantu. Koma nati, Tshimene tshiri tshiani kwa ife?
yang'ana iwe *ndi tshimene.* Naponya pansi zipinjiri za 5
silivere m' malo oyera, ndimo namuka; ndimo nang'ka
nadzimanga nkosi latshi. Ndimo adzukuru akuru natenga 6
zipinjiri za silivere, nati, Si tshamau ku ika izi m' bokosi
la ndrama, tshifuka kuti ziri ntengo wa mwazi. Nafunsana, 7
nagula ndi izo munda wa muntu waomba mbia, ku ika
mianda ya olendo. Mwa kuti munda umene unatshedwa, 8
Munda wa mwazi, ku siku limene. Ndimo anadzazidwa 9
omwe ananenedwa ndi Yeremiya mprofeti, kuti, Ndimo
natenga zipinjiri makumi atatu za silivere, ntengo wa emwe
wawereng'jeredwa, emwe *ena* a ana a Sirayeli anawereng'-

10 jera; ndimo napatsa izo kwa munda wa muntu waomba
mbia, monga Mwini wauza ine.
11 Ndimo Yesu naima patsogolo pa mbiri: ndimo mbiri
namfunsa, kuti, Kodi suli Fumu Yotshuka ya Ayuda?
12 Ndimo Yesu nanena nai', Uti. Ndimo ntawi anatshulidwa
13 ndi adzukuru akuru ndi akuru, sanaiang'ka kantu. Pomwe
Pilato anena nai', Kodi sumva zintu zingati amariza pa iwe?
14 Ndimo sanaiang'ka ie kantu, inde si mau amodzi: monga
15 kuti mbiri nazizwa kwambiri. Ndimo pa kudia mbiri
nakala ku masula kwa antu ambiri womangidwa modzi,
16 emwe anafuna. Ndimo pa ntawi imeneyo anali ndi woma-
17 ngidwa wodziwika, atshedwa Baraba. Ndimo ntawi ana-
song'kanidwa, Pilato nanena nao, Ndani mufuna kuti dima-
sule kwa inu? Baraba, kapena Yesu emwe atshedwa
18 Kristu? Kuti nadziwa kuti kwa dano anapereka ie.
19 Ndimo ntawi analikukala pa mpando wa kuweruza, nkazi
watshi natumiza kwa ie, kuti, Mupotshera palibe kantu ku
tshita ndi muntu wodeka amene: kuti lero dinamva zintu
20 zambiri m' kulota tshifuka tsha ie. Koma adzukuru akuru
ndi akuru nakantshizira antu ambiri kuti anangofunsa Baraba,
21 ndi ku mwaza Yesu. Koma mbiri naiang'ka nanena nao,
Uti wa awiri mufuna kuti dimasule kwa inu? Ndimo
22 nati, Baraba. Pilato anena nao, Ndimo didzatshita tshiani
ndi Yesu emwe atshedwa Kristu? Onse anena, Apatshi-
23 kidwe. Ndimo nati, Bwanje, tshaipa ndi tshiani anatshita?
24 Koma napfula kopambana, kuti, Apatshikidwe. Ndimo
ntawi Pilato naona kuti sanadziwa ku pambanitsa kantu,
koma kopambana kuti pokoso lirikuuka, natenga madzi,
nasamba manja atshi patsogolo pa antu ambiri, kuti, Diri
wopanda kantu ndi mwazi wa muntu wodeka amene:
25 Yang'anirani *iwo.* Ndimo antu onse naiang'ka nati, Mwazi
26 watshi *ukale* pa ife, ndi pa ana atu. Pomwe namasula ku awo
Baraba: koma anakwapula Yesu napereka *ie* ku patshikidwa.
27 Pomwe ankhondo a mbiri natenga Yesu mwa Pretorium,
28 nasong'kanitsa kwa ie gulu lonse la ankhondo. Ndimo
29 nabvula ie, nabveka ie mwinjiro wofira. Ndimo analuka
tshisoti tshotshuka tsha minga, natshiika pa mutu watshi,
ndi nzengo m' dzanja latshi lamanja; nagwada patsogolo
pa ie, nazunza ie, kuti, A, Fumu Yotshuka ya Ayuda!
30 Nalabvula mate pa ie, natenga nzengo nagogoda ie pa mutu.
31 Ndimo ntawi anazunza ie, nabvula mwinjiro kwa ie, nabveka
nsaru zatshi pa ie, namtsogoza kumpatshika.

Ndimo monga analikuturuka, napeza muntu wa Kirene, 32
dzina latshi Simon: emwe nakakaniza ku enda *nao* kuti
anangonyamula nkhwitshi yatshi. Ndimo ntawi anadza ku 33
malo atshedwa Golgota, lomwe liri ku nena, Malo a pala,
napatsa ie vinyo ku mwa wosang'kanizidwa ndi ndulo: ndimo 34
ntawi analawa, sanafuna ku mwa. Ndimo ntawi anapa- 35
tshika ie, nagawana miinjiro yatshi mwa iwo, kuyesa: ndimo 36
nakala pansi nadikira ie apo. Naika pamwamba pa 37
mutu watshi kutshula kwatshi kulembedwa, AMENE ALI
YESU FUMU YOTSHUKA YA AYUDA. Pomwe olanda awiri 38
apatshikidwa ndi ie, modzi pa dzanja latshi lamanja, ndi
modzi pa lamanzere. Ndimo awo omwe anapita namtu- 39
kwana, kupukusa mitu yao, ndi kuti, Iwe emwe umwaza 40
malo oyera, ndimo uamanga m' masiku atatu, udzipulumutse:
ngati uli Mwana wa Mulungu, tsika pa nkhwitshi. Ndimo 41
tshointsho onso adzukuru akuru ku*m*tonza, ndi akulembera
ndi akuru, nati, Napulumutsa ena; wosadziwa ku pulumutsa 42
ie eka. Ali Fumu Yotshuka ya Sirayeli; leka ie tsopano
ku tsika pa nkhwitshi, ndimo tidzamvana ndi ie. Amvana 43
ndi Mulungu; leka ie kumpulumutsa tsopano, ngati amfuna:
kuti nati, Diri Mwana wa Mulungu. Ndimo olanda anso 44
omwe napatshikidwa nai', natonza ie.

Ndimo kwa ora latshisanu ndi tshimodzi kunali ndima pa 45
dziko lonse kwa ora latshisanu ndi tshinai. Ndimo pa ora 46
latshisanu ndi tshinai Yesu napfula ndi liu lalikuru, kuti,
Eloyi, Eloyi, lama sabakatani? lomwe liri, Mulungu wanga,
Mulungu wanga, unandisia bwanje? Ndimo ena a omwe 47
naima apo, ntawi anamva, nati, Muntu amene aitana Eliya.
Ndimo tsopano lino modzi wa awa natamanga, natenga 48
sponje, nalidzaza ndi vinegre, naliika pa nzengo, napatsa ie
ku mwa. Ndimo ena nati, Lekani; tione ngati Eliya adza 49
kumpulumutsa. Ndimo Yesu anapfula anso ndi liu lalikuru, 50
nabweza nzimu watshi. Ndimo ona, tshopimba tsha malo 51
oyera tshinaganikana kawiri kumwamba ku pansi; ndi
dziko linantentemera; ndi matantwe nabanduka; ndi mianda 52
inatsegulidwa; ndi mitembo yambiri ya oyera omwe ana-
gona nadzukitswa; ndimo kuturuka m' mianda pambuiu 53
pa kuukirira kwatshi naloa m' mzinda woyera nadzisonya kwa
ambiri. Ndimo kenturione, ndi awo omwe anali nai' kudi- 54
kira Yesu, ntawi naona tshibvomezi, ndi zintu zomwe zina-
tshitidwa, naopa kwambiri, kuti, Amene anali Mwana wa
Mulungu nditu. Ndimo akazi ambiri anali apo kuyang'ana 55

kutali, omwe anatsata Yesu kwa Galileya, kuimirira kwa ie:
56 mwa omwe anali Mariya kwa Magadala, ndi Mariya amai
ao a Yakobi ndi Yose, ndi amai ao a ana a Zebediya.
57 Ndimo ntawi madzulo anafika, nadza muntu wolemera
kwa Arimateya, atshedwa Yosefe, iemwe enso anali
58 wopunzira wa Yesu: muntu amene nang'ka kwa Pilato,
napempa ntembo wa Yesu. Pomwe Pilato nauza iwo ku
59 perekedwa. Ndimo Yosefe natenga ntembo, naukuta m'
60 nsaru ya lini yotsuka, nauika m' mwanda watshi watsopano,
womwe unafulidwa m' tantwe: nagubuduza mwala woukuru
61 ku komo la mwanda, namuka. Ndimo anali apo Mariya
wa Magadala, ndi Mariya wina kukala pansi pandunji ndi
mwanda.
62 Ndimo pa mawa, lomwe liri *siku* pambuiu Kukonzetsa,
adzukuru akuru ndi Afarisi anasong'kanidwa kwa Pilato,
63 kuti, Fumu, tikumbukila kuti watshinyengo amene nati,
ntawi anali kosuntira ndi moyo, Pambuiu masiku atatu
64 diuka anso. Ndimo uuze kuti mwanda upangidwa
wolimbika kwa siku latshitatu, kani kapena akupunzira
atshi adza namba, nanena ndi antu, Anaukitswa kwa akufa:
ndimo tshimo lakutungo lidzakala loipa lopambana la-
65 patsogolo. Pilato nanena nao, Muli ndi akudikira: mukani,
66 pangani iwo wolimbika monga mudziwa. Ndimo namuka,
napanga mwanda wolimbika, kusindikiza mwala, akudikira
ali nao.
28 Mwa pakupita pa siku la sabata, monga kuamba kutsha
kwa *siku* loamba la wiki, nadza Mariya kwa Magadala ndi
2 Mariya wina ku ona mwanda. Ndimo ona, kunali tshi-
bvomezi tshatshikuru; kuti njelo wa Mwini natsika
3 kumwamba, nadza nafumula mwala, nakala pa iwo. Nkope
yatshi inali monga mpezi, ndi nsaru zatshi zoyera monga
4 khungu: ndimo kwa kuopa kwa ie akudikira nantuntumira,
5 nakala monga antu akufa. Ndimo njelo naiang'ka nanena
ndi akazi, Musaopa inu: kuti didziwa kuti mufuna Yesu,
6 emwe wapatshikidwa. Siali pano; kuti anauka, inde
monga nati. Idzani, ona malo pomwe Mwini nagona.
7 Ndimo mukani nsanga, ndimo uzani akupunzira atshi,
Anauka kwa akufa; ndimo ona, apita patsogolo pa inu m'
8 Galileya; apo mudzamona: ona, danena ndi inu. Ndimo
natshoka nsanga ku mwanda ndi kuopa ndi tshimwemwe
tshambiri, natamanga ku tengera mau ku akupunzira atshi.
9 Ndimo ona, Yesu nakomana nao, kuti, Kalani bwino.

Ndimo nadza nagwira mapazi atshi, nampembedza. Pomwe 10
Yesu anena nao, Musaopa: mukani uzani abali anga kuti
amuke m' Galileya, ndimo apo adzaona ine.

Ndimo ntawi analikumuka, ona, ena a akudikira nadza 11
muzinda nauza adzukuru akuru zintu zonse zomwe zina-
tshitidwa. Ndimo ntawi anasong'kanidwa ndi akuru, ndimo 12
anafunsana, anapatsa ndrama zambiri ku ankhondo, kuti, 13
Uzani, Akupunzira atshi nadza usiku, naba ie ntawi ti-
nagona. Ndimo ngati amene adza ku makutu a mbiri, 14
tidzafulumiza ie, ndimo tidzatshotsa maganizo kwa inu.
Ndimo natenga ndrama, natshita monga anapunzitsidwa: 15
ndimo mau amene anabukidwa mwa Ayuda, *ndimo akalabe*
ku siku limene.

Koma akupunzira kumi ndi modzi nang'ka m' Galileya, 16
ku piri lomwe Yesu anasonyeza awo. Ndimo ntawi 17
namona, na*m*pembedza: koma ena naganizaganiza. Ndimo 18
Yesu nadza ku awo nanena nao, kuti, Mpamvu yonse
yapatsidwa kwa ine m' mwamba ndi pa dziko. Ndimo 19
endani, punzitsani mitundu yonse, kubapatiza awo m' dzina
la Atate ndi la Mwana ndi la Nzimu Woyera: kupunzitsa 20
awo ku sunga zintu zonse zomwe dinauza inu: ndimo ona,
diri ndi inu masiku onse, inde kwa kumariza kwa
kugonera.

---

# IVANGELI WA MARKO.

KUAMBA kwa ivangeli wa Yesu Kristu, Mwana 1
wa Mulungu.

Inde monga alembedwa m' Yesaya mprofeti, 2
Ona, dituma ntenga wanga patsogolo pa nkope yako,
Emwe adzakonzetsa njira yako;
Liu la modzi kulira m' tshipululu, 3
Fotokozani njira ya Mwini,
Pangani njira zatshi zolungama;

Yohane nadza, emwe anabapatiza m' tshipululu nauza 4
mbapatisma la kutembenuza ntima kwa kubweza kwa

5 zimpulupulu. Ndimo naturuka kwa ie dziko lonse la
Yudeya, ndi onse omwe a Yerusalem; ndimo nabapatizidwa
ndi ie m' ntsinje Yordan, kubvumbula mpulupulu zao.
6 Ndimo Yohane wabvala ndi ubwea wa gamila, nali ndi
lamba la tshikopa m' tshunu mwatshi, ndimo nadia madzo-
7 mbe ndi utshi wa muntengo. Ndimo nauza, kuti, Ali-
nkudza pambuiu pa ine iemwe ali wampamvu wopambana
ine, zingwe za dzikwakwata dzatshi sindiri woenera ku
8 weramira ku masula. Dinabapatiza inu ndi madzi; koma
ie adzabapatiza inu ndi Nzimu Woyera.
9 Ndimo kunali m' masiku adya, kuti Yesu anadzera ku
Nazarete wa Galileya, nabapatizidwa ndi Yohane m' Yordan.
10 Ndimo tsopano lino kubvuka ku madzi, naona miamba
inatsegulidwa, ndi Nzimu monga njiwa nutsika pa ie:
11 ndimo liu linadzera ku miamba, Uli Mwana wanga wondi-
konda, mwa iwe disekera bwino.
12 Ndimo tsopano lino Nzimu umtsogoza m' tshipululu.
13 Ndimo anali m' tshipululu masiku makumi anai nayesedwa
ndi Satana; ndimo anali ndi zirombo; ndi anjelo anaimirira
ie.
14 Koma pambuiu pomwe Yohane naperekedwa, Yesu nadza
15 ku Galileya, kuuza ivangeli wa Mulungu, ndimo kuti,
Ntawi idzazidwa, ndi dziko la Mulungu liandikila: tembe-
nuzani mitima yanu, ndimo mvanani m' ivangeli.
16 Ndimo kupita mbali mwa nyanja ya Galileya, naona
Simon ndi Andreya mpwatshi wa Simon kuponya koka m'
17 nyanja: kuti anali apodzo. Ndimo Yesu nanena nao,
Idzani pambuiu pa ine, ndimo didzapanga inu ku kala
18 apodzo a antu. Ndimo tsopano lino anasia maukonde,
19 namtsata. Ndimo kuenda pang'ono, naona Yakobi *mwana*
wa Zebediya, ndi Yohane mpwatshi, omwe enso anali m'
20 tshombo kusoka maukonde. Ndimo tsopano lino anaitana
awo: ndimo nasia atatu ao Zebediya m' tshombo ndi
olipidwa, naenda pambuiu pa ie.
21 Ndimo naloa m' Kapernahum; ndimo tsopano lino pa
22 dzua la sabata naloa m' sinagoge napunzitsa. Ndimo
nazizwa ndi kupunzitsa kwatshi: kuti napunzitsa awa
monga ali ndi mpamvu, ndimo si monga akulembera.
23 Ndimo tsopano lino anali m' sinagoge mwao muntu ndi
24 nzimu wosatsuka; ndimo napfula, kuti, Tiri ndi tshiani ndi
iwe, Yesu wa Nazarete? Kodi udza kutimwaza? diku-
25 dziwa emwe uli, Woyera wa Mulungu. Ndimo Yesu

nausulumula, kuti, Tontola, ndimo turuka kwa ie. Ndimo 26
nzimu wosatsuka, unampikanyikitsa nupfula ndi liu lali-
kuru, unaturuka kwa ie. Ndimo onse anazizwa, monga 27
kuti nafunsana, kuti, Tshiani tshiri tshimenetshi? kupu-
nzitsa kwatsopano! ndi mpamvu auza inde mizimu yosatsuka,
ndimo imvera ie. Ndimo mbiri ya ie inaturuka tsopano 28
lino m' malo onse m' dziko lonse la Galileya lozungulira.

Ndimo tsopano lino, ntawi anaturuka m' sinagoge, naloa 29
m' nyumba ya Simon ndi ya Andreya, ndi Yakobi ndi
Yohane. Koma amai atshi a nkazi wa Simon anagona 30
nadwala malungo; ndimo tsopano lino amuza ndi ie: ndimo 31
nafika nagwira ie ndi dzanja latshi, namtukula; ndimo
malungo namleka, ndimo naimirira kwa awa.

Ndimo madzulo, ntawi dzua lirikuloa, natenga kwa ie 32
onse omwe analikudwala, ndi awa omwe anagwidwa ndi
ademon. Ndimo mzinda wonse unasong'kanidwa ku komo. 33
Ndimo natshiritsa ambiri omwe analikudwala ndi ntenda 34
zolekana, naturutsa ademon ambiri; ndimo sanaleka
ademon ku lankula, tshifuka anamdziwa.

Ndimo m' mamawa, ntawi yeikuru patsogolo pa kuamba 35
poyera, nauka naturuka, nang'ka ku tshipululu, ndimo uko
napempera. Ndimo Simon ndi awo omwe anali nai' 36
namtsata; ndimo anampeza, ndimo anena nai', Onse aliku- 37
funa iwe. Ndimo anena nao, Tidzing'ke ku malo ena 38
ku midzi, yakuandikana, kuti diuze apo onso; kuti
kwa tshifukwa tshimene dinaturuka. Ndimo naloa m' 39
masinagoge ao mwa Galileya lonse, kuuza ndi kuturutsa
ademon.

Ndimo adza kwa ie wakate, kupempa ie, ndimo kugwada 40
kwa ie, ndimo kunena ndi ie, Ngati ufuna, udziwa
kundisambitsa. Ndimo anali ndi tshisoni mutima, naturutsa 41
dzanja latshi, natosa ie, ndimo anena nai', Difuna; sambitsi-
dwa. Ndimo tsopano lino kate linatshoka kwa ie, ndimo 42
nasambitsidwa. Ndimo anamuza kwambiri, ndimo tsopano 43
lino namtumiza, ndimo anena nai', Yang'ana usanena kantu 44
kwa muntu modzi: koma muka, sonyeza iwe eka kwa
ndzukuru, nutsira kwa kusambitsa kwako zintu zomwe
Moses nauza, kwa kumariza ku awa. Koma anaturuka, 45
naamba ku uza kwambiri, ndi ku bukitsa mau, tshointshi
kuti Yesu sanadziwa ku loa poyera muzinda, koma anali
kunja m' malo atshipululu: ndimo anasong'kana kwa ie kwa
malo onse.

2 Ndimo ntawi naloa anso m' Kapernahum pambuiu pa
2 masiku ena, ananenedwa kuti anali m' nyumba, ndimo
ambiri anasong'kanidwa, monga kuti kunalibe malo *kwa*
*awo*, iai, si inde pa komo: ndimo nanena mau kwa awo.
3 Ndimo adza, kutenga kwa ie muntu wodwala wonjenjemera,
4 ananyamulidwa ndi anai. Ndimo ntawi sanadziwa ku fika
pafupi kwa ie tshifuka tsha antu ambiri, nabvundukula
tshindu pomwe anali: ndimo ntawi nalisasula, natsitsa kama
5 pomwe wodwala wonjenjemera anagona. Ndimo Yesu
kuona mvanu wao anena ndi wodwala wonjenjemera,
6 Mwana, zakwaipa zako zikululukiridwa. Koma anali ena
a akulembera nakala pansi apo, ndimo kusing'kasing'ka m'
7 mitima yao, Bwanje muntu amene anena tshointsho? atu-
kwana *Mulungu:* ndani adziwa ku kululukira zakwaipa
8 koma modzi, *inde* Mulungu? Ndimo tsopano lino Yesu,
kudziwitsa m' nzimu watshi kuti anasing'kasing'ka
tshointshi m' awa oka, anena nao, Bwanje musing'kasing'ka
9 zintu zimenezi m' mitima yanu? Tshiti tshiri tshopepuka,
ku nena kwa wodwala wonjenjemera, Zakwaipa zako ziku-
lulukidwa; kapena ku nena, Uka, tenga kama wako,
10 nuenda? Koma kuti mudziwe kuti Mwana wa muntu ali
ndi mpamvu pansi pano ku kululukira zakwaipa (anena ndi
11 wodwala wonjenjemera), Dinena ndi iwe, Uka, tenga kama
12 wako, ndimo muka ku nyumba yako. Ndimo nauka, ndimo
tsopano lino natenga kama, naturuka patsogolo pa onse;
monga kuti onse anazizwa, napambanitsa Mulungu, kuti,
Sitinaona ntawi ina tshimwetshi.
13 Ndimo naturuka anso mbali mwa nyanja; ndimo antu
ambiri onse nasong'kana kwa ie, ndimo napunzitsa awo.
14 Ndimo monga napita, naona Levi *mwana* wa Alifeyu kukala
pa malo polandira tsong'ko, ndimo anena nai', Tsata ine.
15 Ndimo nauka namtsata. Ndimo kunali, kuti analikukala
pa kudia m' nyumba mwatshi, ndimo olandira tsong'ko
ambiri ndi ampulupulu nakala ndi Yesu ndi akupunzira
16 atshi: kuti anali ambiri, ndimo namtsata. Ndimo akulembe-
ra a Afarisi, ntawi naona kuti analinkudia ndi ampulupulu
ndi olandira tsong'ko, nanena ndi akupunzira atshi, Adia ndi
17 ku mwa ndi olandira tsong'ko ndi ampulupulu. Ndimo
ntawi Yesu anamva, anena nao, Awa omwe ali olimba osali
ndi kufunidwa ndi sing'anga, koma awa omwe ali odwala:
Dinafika si ku itana odeka, koma ampulupulu.
18 Ndimo akupunzira a Yohane ndi Afarisi analeka kudia;

ndimo adza kunena nai', Akupunzira a Yohane ndi akupu-
nzira a Afarisi aleka kudia bwanje, koma akupunzira ako
osaleka kudia? Ndimo Yesu nanena nao, Kodi mapungu 19
adziwa ku leka kudia, ntawi wokwati ali nao? ntawi
yomwe ali ndi wokwati, osadziwa ku leka kudia. Koma 20
masiku adzadza, ntawi wokwati adzatshotsedwa kwa awa,
ndimo pomwe adzaleka kudia m' siku limene. Palibe 21
muntu asoka tshigamba tsha nsaru tshatsopano pa maraia
akali: kani tshimene tshomwe tshikakwanira tshitshotsa kwa
iwo, tshatsopano kwa akali, ndimo tshibo tshatshikuru
tshipangidwa. Ndimo palibe muntu atsira vinyo watsopano 22
m' dzikopa dzakali: kani vinyo adzang'amba dzikopa, ndimo
vinyo amwazika, ndimo dzikopa: koma *atsira* vinyo
watsopano m' dzikopa dzatsopano.

Ndimo kunali, kuti analikupita pa dzua la sabata mwa 23
minda ya dzintu; ndimo akupunzira atshi naamba, monga
napita, kukadzula ngala za dzintu. Ndimo Afarisi nanena 24
nai', Ona, atshita bwanje pa dzua la sabata tshimene
tshomwe si tshiri tshamau? Ndimo nanena nao, Kodi 25
musanawerenga ntawi ina tshomwe Davide natshita, ntawi
nasoa, namva njala, ie, ndi awa omwe anali nai'? Bwanje 26
naloa m' nyumba ya Mulungu ntawi Abiyatre anali
ndzukuru wang'kuru, ndimo nadia mikate yoonetsa, yomwe
siiri yamau ku dia koma kwa adzukuru, napatsa anso ku
awa omwe anali nai'? Ndimo nanena nao, Sabata 27
linapangidwa kwa muntu, ndimo si muntu kwa sabata:
tshointsho kuti Mwana wa muntu ali mwini inde wa 28
sabata.

Ndimo naloa anso m' sinagoge; ndimo umo munali 3
muntu emwe anali ndi dzanja latshi lokwinyata. Ndimo 2
anayang'anira ie, ngati akatshiritsa ie pa dzua la sabata;
monga anangotshula ie. Ndimo anena ndi muntu emwe 3
anali ndi dzanja lokwinyata, Uka, *uli* pakati. Ndimo anena 4
nao, Kodi si tshamau pa siku la sabata ku tshita tshabwino
kapena ku tshita mpingo? ku pulumutsa moyo, kapena ku
pa? Koma natontola. Ndimo ntawi anayang'anitsa pa 5
awo ndi kukwia, ali ndi tshisoni m' ntima ndi kulimbikitsa
kwa mitima yao, anena ndi muntu, Turutsa dzanja lako.
Ndimo analiturutsa: ndimo dzanja latshi linafotokozedwa.
Ndimo Afarisi naturuka, ndimo tsopano lino ndi Aherode 6
naweruzana pa ie, bwanje anangomwononga.

Ndimo Yesu ndi akupunzira atshi nadzibweza ku nyanja: 7

ndimo antu ambiri kwa Galileya anatsata: ndimo kwa
8 Yudeya, ndimo kwa Yerusalem, ndimo kwa Idumeya,
ndimo patsidia pa Yordan, ndimo azunguniza Tire ndi
Tsidon, antu ambiri, anamva zintu zazikuru zomwe nazi-
9 tshita, nadza kwa ie. Ndimo nanena ndi akupunzira atshi,
kuti katshombo kakalindira ie tshifuka tsha antu ambiri,
10 kani akaunjikana ie: kuti anatshiritsa ambiri; tshointsho
kuti monga ambiri monga anali ndi dzaola anaunjikana ie
11 kuti anangotosa ie. Ndimo mizimu yosatsuka, ntawi inaona
ie, inagwa patsogolo pa ie, ndimo inapfula, kuti, Iwe uli
12 Mwana wa Mulungu. Ndimo nauza iyo kolimba kuti
siikamdziwitsa.
13 Ndimo akwera pa piri, ndimo aitana kwa ie omwe
14 ie eka afuna: ndimo namuka kwa ie. Ndimo anapakula
kumi ndi awiri, kuti anangokala nai', ndimo kuti ana-
15 ngotumiza awo ku uza, ndimo ku potshera mpamvu ku
16 turutsa ademon: ndimo Simon wasintanitsa Petros;
17 ndimo Yakobi *mwana* wa Zebediya, ndi Yohane mpwatshi
wa Yakobi; ndi awo wasintanitsa Bowanerges, lomwe liri,
18 Ana a bingu: ndimo Andreya, ndi Filipu, ndi Bartolomeyu,
ndi Mateyu, ndi Tomas ndi Yakobi *mwana* wa Alifeyu, ndi
19 Tadeyu, ndi Simon Mkanane, ndi Yuda Sikariyoti, emwe
enso anamzonda.
20 Ndimo aloa m' nyumba. Ndimo antu ambiri asong'kana
21 anso, monga kuti sanadziwa konse ku dia nkate. Ndimo
ntawi abali atshi anamva, naturuka kumgwira: kuti nanena,
22 Nzeru zinamsia. Ndimo akulembera omwe natsika kwa
Yerusalem anati, Apotshera Belzebule, ndimo, Ndi wo-
23 weruza wa ademon aturutsa ademon. Ndimo anaitana awo
kwa ie, nanena nao m' mafanizo, Satana adziwa ku turutsa
24 Satana bwanje? Ndimo ngati dziko ligawidwa pa loka,
25 dziko limene silidziwa ku ima. Ndimo ngati banja
ligawidwa pa loka, banja limene silidzadziwa ku ima.
26 Ndimo ngati Satana wauka pa eka, ndimo wagawidwa,
27 wosadziwa ku ima, koma apotshera nsonga. Koma palibe
modzi adziwa ku loa m' nyumba ya *muntu* wolimba, ku
ononga zintu zatshi, ngati poiamba amanga *muntu* wolimba;
28 ndimo pomwe adzaononga nyumba yatshi. Dinena ndi inu
nditu, Zakwaipa zonse zao zidzakululukidwa kwa ana a
29 antu, ndi matukwano ao ndi omwe adzatukwana: koma
iemwe adzatukwana pa Nzimu Woyera palibe ntawi ina
apotshera kukululukidwa, koma ali wotshimwa wa mpulu-

pulu yosamariza: tshifuka nanena, Apotshera nzimu 30
wosatsuka.

Ndimo adza amai atshi ndi abali atshi; ndimo, kuima 31
kunja, natumiza kwa ie, namwitana. Ndimo antu ambiri 32
analikukala pansi kozunguniza ie; ndimo anena nai', Ona,
amai ako ndi abali ako kunja afuna iwe. Ndimo aiang'ka 33
awo, ndimo ati, Ndani ali amai anga ndi abali anga?
Ndimo kuyang'anayang'ana pa awo omwe nakala pansi 34
kozunguniza ie, anena, Ona, amai anga ndi abali anga!
kuti iemwe adzatshita kufuna kwa Mulungu, iemwe ali 35
mpwanga, ndi mlongo*wanga*, ndi amai *anga*.

Ndimo onso naamba ku punzitsa mbali mwa nyanja. 4
Ndimo asong'kanidwa kwa ie antu ambiri nditu, monga
kuti naloa m' tshombo, nakala m' nyanja; ndimo antu onse
ambiri anali mbali mwa nyanja pa ntunda. Ndimo napu- 2
nzitsa awo zintu zambiri m' mafanizo, nanena nao m'
kupunzitsa kwatshi, Imvani: Ona, wofesa naturuka ku 3
fesa: ndimo kunali, monga nafesa, *mbeu* ina inagwa mbali 4
mwa njira, ndi mbalame zinadza ndi zinaidia. Ndimo ina 5
inagwa pa *ntaka* yatantwe, pomwe siinali ndi ntaka yambiri;
ndimo tsopano lino inamera, tshifuka siinali ndi ntaka
yakuya: ndimo ntawi dzua linali kumwamba, inanyali- 6
tsidwa; ndimo tshifuka inali yopanda ntsitsi, inakwinyata.
Ndimo ina inagwa mwa minga, ndimo minga inamera, 7
nikwinyatitsa, ndimo siinabala mitolo. Ndimo zina zinagwa 8
mwa ntaka yabwino, ndimo zinabala mitolo, kumera ndi
kukula; ndimo zinamasula, makumi atatu, ndi makumi
asanu ndi limodzi, ndi makumi okaoka kumi. Ndimo 9
nanena, Iemwe ali makutu ku mva, amve.

Ndimo ntawi anali eka, awo omwe anali nai', ndi kumi ndi 10
awiri anamfunsa mafanizo. Ndimo nanena nao, Ku inu 11
kupatsidwa kusadziwika kwa dziko la Mulungu: koma kwa
awo omwe ali kunja, zintu zonse zipangidwa m' mafanizo:
kuti kuona angoona ndi osadziwitsa; ndi kumva ango- 12
mva, ndi osamvetsa; kani kapena akatembenuza anso,
ndimo tshikakulululukiridwa ku awo. Ndimo anena nao, 13
Kodi simudziwa fanizo limene? ndimo bwanje mudzadziwa
mafanizo onse? Wofesa afesa mau. Ndimo amene ali 14, 15
omwe mbali mwa njira, pomwe mau afesedwa; ndimo
ntawi anamva, tsopano lino Satana adza, ndimo atshotsa
mau omwe anafesedwa mwao. Ndimo amene modzimodzi 16
ali omwe afesedwa pa *malo* atantwe, omwe, ntawi anamva

17 mau, tsopano lino alandira ndi tshimwemwe; ndimo osapo-
tshera ntsitsi m' awo oka, koma akalabe kantawi; pomwe,
ntawi sautso kapena zunzo ziuka tshifuka tsha mau, tsopano
18 lino akwiitsa. Ndimo ena ali omwe afesedwa mwa minga;
19 amene ali omwe anamva mau, ndimo maganizo a kugonera,
ndi tshinyengo tsha zolemera, ndi mafuno a zintu zina kuloa,
20 zikwinyatitsa mau, ndimo akala kosabala. Ndimo amene
ali omwe anafesedwa pa ntaka yabwino; otere monga amva
mau, nalandira, nabala mitolo, makumi atatu, ndi makumi
asanu ndi limodzi, ndi makumi okaoka kumi.

21 Ndimo nanena nao, Kodi nyali itengedwa ku ikidwa pansi
pa ntanga, kapena pansi pa kama, *ndimo* si ku ikidwa pa
22 tshogwira nyali? Kuti kulibe kantu kobisala, koma kuti
kadzasonyezedwa; kapena *kantu* kanabisidwa, koma kuti
23 kadzaonetsa. Ngati muntu modzi ali makutu ku mva, amve.
24 Ndimo nanena nao, Yang'ana ndi tshomwe mumve: ndi
muyezo womwe muyeza udzayezedwa kwa inu: ndimo
25 kopambana kadzapatsidwa kwa inu. Kuti iemwe apotshera,
ku ie adzapatsidwa: ndimo iemwe wosapotshera, kwa ie
tshidzatshotsedwa inde tshomwe ali natsho.

26 Ndimo anati, Tshointshi liri dziko la Mulungu, monga
27 ngati muntu akafesa mbeu pa ntaka; ndimo akagona
nakauka usiku ndi nsana, ndimo mbeu ikamera nikakula,
28 wosadziwa bwanje. Dziko libala dzobala kwa loka;
poiamba kakwata, ndimo ngala, pomwe yatsha ngala.
29 Koma ntawi dzobala dzipsa, tsopano lino atema ndi mpeni,
tshifuka kukung'ka kwafika.

30 Ndimo anati, Tidzafaniza lanje dziko la Mulungu?
31 kapena m' fanizo lanje tidzaliika? Monga mpetshe ya
mostade, yomwe, ntawi ifesedwa pa ntaka, ngati iri yeing'-
32 ono ndi mbeu zonse zomwe ziri pa ntaka, kosuntira ntawi
ifesedwa, imera, nikala yeikuru yopambana misipu yonse,
nibaluka ntambi zazikuru; monga kuti mbalame zaku-
mwamba zingokala pansi pa ntunzi wa iyo.

33 Ndimo ndi mafanizo ambiri otere nanena nao mau, monga
34 anadziwa ku mva: ndimo lopanda fanizo sananena nao:
koma kutseri ku akupunzira atshi nasonyeza zintu zonse.

35 Ndimo pa dzua limene, ntawi madzulo anadza, anena nao,
36 Tiyambuke kutsidia lina. Ndimo kusia antu ambiri,
anamtenga nao, inde monga anali, m' tshombo. Ndimo
37 dzombo dzina dzinali ndi ie. Ndimo uuka mondwe
woukuru wa mpepo, ndimo mafunde analikugabvikira m'

tshombo, tshointshi kuti tsopano tshombo tshinalikudzaza.
Ndimo ie eka anali ku makaliro kwa tshombo, nagona pa 38
ntsamiro: ndimo amgalamutsa, ndimo anena nai' Mpunzitsi,
usasamala kuti timwazika? Ndimo nagalamuka, nasulumula 39
mpepo, nanena ndi nyanja, Tontola, kala bata. Ndimo
mpepo inaleka, ndimo linali bata lalikuru. Ndimo nanena 40
nao, Bwanje muli oopa? kodi kosuntira musali ndi mvanu?
Ndimo naopa kwambiri, nauzana, Nanga amene ali ani, 41
kuti inde mpepo ndi nyanja zimvera ie?

Ndimo anafika patsidia lina la nyanja, kwa dziko la 5
Agerasa. Ndimo ntawi anaturuka m' tshombo tsopano lino 2
nakomana nai' kwa mianda mamuna ndi nzimu wosatsuka,
emwe anali ndi malo atshi m' mianda: ndimo kulibe muntu 3
anadziwa kummanga ntawi ina, iai, si ndi unyolo; tshifuka 4
kuti anamangidwa ntawi zambiri ndi magrigadyera ndi
maunyolo, ndimo maunyolo anadudwa ndi ie, ndimo
magrigadyera nadudwa m' zipinjiri: ndimo kulibe muntu
ali ndi mpamvu kumzolowera. Ndimo ntawi zonse, usiku 5
ndi nsana, m' mianda ndi m' mapiri, analikupfula, ndi
kudzitsheka ndi miala. Ndimo ntawi naona Yesu kwa 6
kutali, natamanga napembedza ie; ndimo kupfula ndi liu 7
lalikuru, ati, Ditshita tshiani ndi iwe, Yesu, Mwana wa
Mulungu Wopambanitsa? dilimbika iwe ndi Mulungu,
usandizunza: Kuti nanena nai', Turuka, nzimu wosatsuka, 8
kwa muntu. Ndimo namfunsa, Dzina lako ndi iwe ani? 9
Ndimo unena nai', Dzina langa liri Lijon; kuti tiri yambiri.
Ndimo unamfunsa kwambiri, kuti sakatumiza iyo kunja kwa 10
dziko. Ndimo linali apo pa kundu la piri gulu lalikuru la 11
nkhumba kueta. Ndimo inamfunsa, kuti, Utitumize mwa 12
nkhumba, monga kuti tingoloa mwa izo. Ndimo wabvomera 13
iyo. Ndimo mizimu yosatsuka inaturuka, niloa mwa
nkhumba: ndimo gulu linatsika nsanga malo otseruka m'
nyanja, m' *kuwerenga* kwa mazousan awiri; ndimo zina-
tsekedwa pwea m' nyanja. Ndimo omwe naeta izo natawa, 14
nanena muzinda, ndi m' minda. Ndimo nafika ku ona
tshiani tshinali tshomwe tshinakala. Ndimo adza kwa Yesu, 15
naona iemwe anagwidwa ndi ademon kukala pansi, nabvala
ndi m' nzeru zatshi, *inde* emwe anali ndi lijon: ndimo
naopa. Ndimo omwe anaona nauza kwa awo bwanje anali 16
kwa iemwe anagwidwa ndi ademon, ndimo ndi nkhumba.
Ndimo naamba ku pempa ie ku tshoka kwa maliri ao. 17
Ndimo monga analikuloa m' tshombo, iemwe anagwidwa ndi 18

19 ademon napempa ie kuti anangokala ndi ie. Ndimo sanam-
leka, koma anena nai', Muka ku nyumba yako kwa abali
ako, nuuza awo bwanje zintu zazikuru Mwini watshita kwa
20 iwe, ndimo *bwanje* anali ndi nsisi ndi iwe. Ndimo namuka,
naamba ku uza m' Dekapolis bwanje zintu zazikuru Yesu
anatshita kwa ie : ndimo antu onse nazizwa.
21 Ndimo ntawi Yesu nayambuka anso m' tshombo kutsidia
lina, antu ambiri nasong'kanidwa kwa ie : ndimo anali
22 mbali mwa nyanja. Ndimo adza modzi wa akuru a sinagoge,
dzina latshi Yayiro ; ndimo kuona ie, agwa pa mapazi atshi,
23 nampempa kwambiri, kuti, Kabutu kanga kakang'ono
katofuna ku fa : *dikupempera*, kuti kudza ungoika manja
ako pa iko, kuti kangotshiritsidwa, ndi ku kala ndi moyo.
24 Ndimo naenda nai' ; ndi antu ambiri natsata ie, naunjikana
pa ie.
25 Ndimo nkazi, emwe anali ndi kuka mwazi dzaka kumi
26 ndi dziwiri, ndimo anamva zintu zambiri kwa asing'anga
ambiri, nalipira zatshi zonse, ndimo sanatshiritsidwa kantu,
27 koma nadwala kopambana, anamva zintu ndi Yesu, nadza
28 m' kutitimizana pambuiu, natosa mwinjiro watshi. Kuti
nanena, Ngati ditosa koma miinjiro yatshi, didzatshiritsidwa.
29 Ndimo tsopano lino kasope wa mwazi watshi waumitsidwa ;
ndimo anamva m' tupi latshi kuti anatshiritsidwa wa ntenda
30 yatshi. Ndimo tsopano lino Yesu, kudziwitsa mwa ie eka
kuti mpamvu *kuturuka* kwa ie inaturuka, natembenuka m'
31 kutitimizana, nati, Natosa miinjiro yanga ndani? Ndimo
akupunzira atshi anena nai', Uona antu ambiri atitimiza
32 iwe, ndimo uti, Ndani wanditosa? Ndimo anayang'anayang'-
33 ana ku ona iemwe anatshita tshintu tshimene. Koma nkazi
kuopa ndi kuntentemera, kudziwa tshomwe tshatshitidwa
kwa ie, nadza nagwa patsogolo pa ie, namuza ie nteradi
34 wonse. Ndimo nanena nai', Mwana wankazi, mvanu wako
unakutshiritsa ; muka ndi ntendere, nukala wolimba kwa
ntenda yako.
35 Ntawi kosuntira alikulankula, adza kwa *nyumba ya* mkuru
wa sinagoge, kunena, Mwana wankazi wako wafa : nkhanı
36 inso njanje Mpunzitsi? Koma Yesu, sikusamala mau
ananenedwa, anena ndi mkuru wa sinagoge, Usaopa, mvana
37 koka. Ndimo sanaleka muntu kumtsata, koma Petros, ndi
38 Yakobi, ndi Yohane mpwatshi wa Yakobi. Ndimo adza ku
nyumba ya mkuru wa sinagoge ; ndimo aona pokoso, ndi
39 *ambiri* kulira misozi ndi kupfula kwambiri. Ndimo ntawi

analoa, anena nao, Mupokosera ranje, ndi ku lira misozi?
kamwana sakanafa, koma kagona. Ndimo nanyodola ie. 40
Koma ie, anaturutsa awo onse, atenga atate a kamwana ndi
amai atshi ndi omwe anali nai', naloa pomwe kamwana
kanali. Ndimo kutenga kamwana ndi dzanja, anena nako, 41
Talita kumi; emwe ali, asandukidwa, Kabutu, dinena ndi
iwe, Uka. Ndimo tsopano lino kabutu kanauka, nakaenda- 42
enda; kuti kanali ndi dzaka kumi ndi dziwiri. Ndimo
nazizwa tsopano lino ndi kuzizwa kwambiri. Ndimo nauza 43
awo kwambiri kuti palibe muntu akadziwa tshimene: ndimo
nauza kuti *kantu* kapatsidwe iko ku dia.

Ndimo naturuka uko; ndimo adza ku dziko latshi; ndimo 6
akupunzira atshi amtsata. Ndimo ntawi sabata linadza, 2
naamba ku punzitsa m' sinagoge: ndimo ambiri anamva ie
nazizwa, kuti, Muntu amene ali ndi zintu zimenezi kuti?
ndimo, Nzeru iri yanje yomwe ipatsidwa kwa muntu amene,
ndimo *zitantauza zanje* mpamvu zotere zitshitidwa ndi
manja atshi? Kodi amene siali misiri wa mitengo, mwana 3
wa Mariya, ndi njiratshi wa Yakobi, ndi Yose, ndi Yuda,
ndi Simon? ndi alongwatshi kodi siali pano ndi ife?
Ndimo anakwiitsidwa ndi ie. Ndimo Yesu nanena nao, 4
Mprofeti siali wopanda ulemu, koma m' dziko latshi, ndi
mwa abali atshi, ndi m' nyumba yatshi. Ndimo apo sana- 5
dziwa ku tshita mpamvu, koma kuti naika manja atshi pa
antu odwala owereng'jeka, natshiritsa awo. Ndimo nazizwa 6
tshifuka tsha kusamvana kwao.

Ndimo napitapita midzi, kupunzitsa.

Ndimo naitana kwa ie kumi ndi awiri, naamba ku tumiza 7
awo awiri ndi awiri; ndimo napatsa awo mpamvu pa mizimu
yosatsuka; naauza monga kuti akatenga kulibe kantu kwa 8
ulendo *wao*, koma ndodo yoka; palibe nkate, palibe tumba,
palibe ndrama m' mpango; koma *ku enda* kubvala ndi 9
dzikwakwata: ndimo, *nati*, musabvala miinjiro iwiri.
Ndimo nanena nao, Malo omwe muloa m' nyumba, kalani 10
apo kwa ntawi mung'ka uko. Ndimo malo omwe sadzafuna 11
ku landira inu, ndimo sadzamva inu, monga ntawi mung'ka
apo, sansani fumbi lomwe liri pansi pa mapazi anu kwa
kumariza kwa awo. Ndimo naturuka, nauza kuti *antu* 12
akatembenuza mitima. Ndimo naturutsa ademon ambiri, 13
nadzosa ndi mafuta ambiri omwe anali odwala, natshiritsa
awo.

Ndimo fumu yotshuka Herode inamva *ndi tshimene;* kuti 14

dzina latshi linabukitsidwa: ndimo nanena, Yohane
Mbapatizi waukirira kwa akufa, ndimo tshointshi mpamvu
15 zimene zitshita mwa ie. Koma ena nati, Ali Eliya.
Ndimo ena nati, *Ali* mprofeti, *inde* monga modzi wa aprofeti.
16 Koma Herode, ntawi anamva, nati, Yohane, emwe dadula
17 mutu watshi, waukirira. Kuti Herode ie eka anatumiza
nagwira Yohane, nammanga m' nyumba ya ndima kwa
Herodiya, nkazi wa njiratshi Filipu: kuti anakwata ie.
18 Kuti Yohane ananena ndi Herode, Sitshiri tshamau kwa iwe
19 ku potshera nkazi wa njirako. Ndimo Herodiya nadzikwiitsa
20 pa ie, ndimo nafuna kumpa; ndimo sanadziwa; kuti Herode
naopa Yohane, kudziwa kuti anali muntu wodeka ndi woyera,
nasungira ie. Ndimo ntawi anamva ie, naganizaganiza kwa-
21 mbiri; namva ie kosekera. Ndimo ntawi siku labwino linafika,
kuti Herode pa siku lobadwa latshi napanga ngonero kwa
22 ambiri atshi, ndi akazembe, ndi akuru a Galileya; ndimo ntawi
mwana wankazi wa Herodiya ie eka naloa nabvina, naseketsa
Herode ndi omwe nadia nai'; ndimo fumu yotshuka inanena
ndi butu, Funsa ine tshomwe ufuna, ndimo didzakupatsa.
23 Ndimo nalumbirira kwa ilo, Tshomwe udzafunsa kwa ine,
24 didzakupatsa, kwa nusu la dziko langa. Ndimo linaturuka,
nanena ndi amai atshi, Difunsa tshiani? Ndimo nati, Mutu
25 wa Yohane Mbapatizi. Ndimo tsopano lino linaloa ndi
nsangu kwa fumu yotshuka, nafunsa, kuti, Difuna kuti pa
ntawi yatsopano undipatse m' mbale yeikuru mutu wa
26 Yohane Mbapatizi. Ndimo fumu yotshuka inali ndi
tshisoni tshambiri; koma kwa malumbiro atshi, ndi kwa
27 omwe adia nai', isanafuna kulikana. Ndimo tsopano lino
fumu yotshuka inatumiza wankhondo wa kudikira kwa-
tshi, nauza ku tenga mutu watshi: ndimo nang'ka nadula
28 mutu watshi m' nyumba ya ndima, natenga mutu watshi m'
mbale yeikuru, naupatsa kwa butu: ndimo butu linaupatsa
29 kwa amai atshi. Ndimo ntawi akupunzira atshi anamva,
nadza nanyamula ntembo watshi, nauika m' mwanda.
30 Ndimo apostile anasong'kana kwa Yesu; nauza ie zintu
31 zonse, zomwe anatshita, ndi zomwe anapunzitsa. Ndimo
anena nao, Idzani inu noka ozemba ku tshipululu, ku puma
kantawi. Kuti anali ambiri kudza ndi kupita, ndimo
32 sanapotshera ntawi yopuma inde ku dia. Ndimo nang'ka
33 m' tshombo ku tshipululu tshozemba. Ndimo *antu* naona
awa kupita, ndi ambiri nadziwa *awa*, natamanga pamodzi
34 pantunda uko kwa mizinda yonse, napitirira awa. Ndimo

naturuka naona antu ambiri, ndimo anali ndi tshisoni
mutima ndi awa, tshifuka anali ofana ndi nkosa zopanda
mbusa: ndimo naamba ku punzitsa awa zintu zambiri.
Ndimo ntawi tsopano dzua linapita kwambiri, akupunzira 35
atshi nadza kwa ie, nati, Malo ali tshipululu, ndi tsopano
dzua linapita kwambiri: tumiza awa, kuti angoenda m' 36
dziko ndi m' midzi zozungulira, kuti angogula kwa awo oka
kantu ku dia. Koma naiang'ka nanena nao, Apatseni adie. 37
Ndimo anena nai', Kodi tidzing'ka ku gula madenariyon
mazana awiri a mikate, tiapatse ku dia? Ndimo anena nao, 38
Mikate ingati muli naiyo? endani ku ona. Ndimo ntawi
nadziwa, ati, Isanu, ndi nsomba ziwiri. Ndimo nauza awa 39
kuti onse akakala pansi ndi magulu pa maudzu obiriwiri.
Ndimo nakala pansi mifunde, ndi mazana, ndi makumi 40
asanu, ndi makumi asanu. Ndimo natenga mikate isanu ndi 41
nsomba ziwiri, ndi kuyang'ana ku mwamba, nadalitsa, naswa
mikate; ndimo napatsa ku akupunzira ku ika patsogolo pa
awa; ndi nsomba ziwiri nagawira onse. Ndimo onse nadia, 42
nakuta. Ndimo natola zinyenyeswa, mitanga kumi ndi 43
iwiri inadzaza, ndi inso za nsomba. Ndi omwe anadia 44
mikate anali amuna mazousan asanu.

Ndimo tsopano lino nafulumiza akupunzira atshi 45
ku loa m' tshombo, ndi ku tsogolera kutsidia lina ku
Betsayida, ntawi ie eka atshotsa antu ambiri. Ndimo 46
pambuiu anatsazika awo, namuka ku piri ku pempera.
Ndimo ntawi madzulo anadza, tshombo tshinali pakati pa 47
nyanja, ndi ie eka pantunda. Ndimo kuona awo kusauka 48
ndi kupalasa, kuti mpepo inali patsogolo pa awo, kwa
kudikira kanai kwa usiku adza kwa awo, kuendaenda pa
nyanja; ndimo nakafuna ku pitirira awo: koma awa, ntawi 49
anamona kuendaenda pa nyanja, naganizaganiza kuti unali
nzukwa, napfula: kuti onse anamona, nantuntumiridwa. 50
Koma tsopano lino nalankula nao, ndimo anena nao, Kalani
osekera: diri ine; musaopa. Ndimo nakwera kwa awo 51
m' tshombo; ndimo mpepo inaleka: ndimo nazizwa
kwambiri mwa awa oka; kuti sanadziwa ndi mikate, kuti 52
mitima yao inalimbikidwa.

Ndimo ntawi anayambuka, nafika ku dziko ku Genesarete, 53
nakotsheza pa doko. Ndimo ntawi naturuka m' tshombo, 54
tsopano lino *antu* namdziwa, natamanga pa dziko lonse lidya 55
lozungulira, naamba ku nyamula pa akama ao omwe anali
odwala, pomwe anamva anali. Ndimo komwe naloa, m' 56

midzi, kapena m' mizinda, kapena m' minda, naika odwala
m' malo a maronda, nampempa kuti anangotosa ngati kunali
inde mtsheu wa mwinjiro watshi: ndimo monga ambiri
monga natosa ie anatshiritsidwa.

7 Ndimo anasong'kana kwa ie Afarisi, ndi ena a akulembera,
2 omwe anadza kwa Yerusalem, ndimo anaona kuti ena a
akupunzira atshi nadia nkate wao ndi manja anko, omwe ali
3 osatsuka. Kuti Afarisi, ndi Ayuda onse, ngati osasamba
manja ao kwatshangu, osadia, kugwira mwambi wa akuru:
4 ndimo *ntawi abwera* ku bwalo la maronda, ngati osasamba,
osadia: ndimo ziripo zintu zina zambiri, zomwe anazila-
ndira kuzigwira, kutsuka kwa ziko, ndi mipika, ndi dziwira
5 dza nkua. Ndimo Afarisi ndi akulembera amfunsa, Bwanje
akupunzira ako osaendaenda ofana ndi mwambi wa akuru,
6 koma adia nkate wao ndi manja anko? Ndimo nanena nao,
Yesaya nalosa bwino ndi inu atshinyengo, monga alembe-
dwa,

Antu amene andilemekeza ndi milomo yao,
Koma mitima yao iri kutali kwa ine.
7 Koma kwautsiru andipembedza,
Kupunzitsa *monga* zopunzitsa *zao* mau a antu.

8 Musia mau a Mulungu, ndimo mugwira mwambi wa antu.
9 Ndimo nanena nao, Bwino mukana mau a Mulungu, kuti
10 mungogwira mwambi wanu. Kuti Moses nati, Lemekeza
atatu ako ndi amai ako; ndimo, Iemwe alankula koipa ndi
11 atatu atshi kapena amai atshi, afe imfa: koma muti, Ngati
muntu adzanena kwa atatu atshi kapena amai atshi, Tshi-
mene ndi tshomwe munangopindulidwa ndi ine tshiri
Korban, tshomwe tshirikunena, Tshapatsidwa *kwa Mulungu;*
12 musamleka ntawi ina ku tshita kantu kwa atatu atshi
13 kapena amai atshi; kupanga mau a Mulungu kwa tshabe
ndi mwambi wanu, womwe munapatsa: ndi zintu zambiri
14 zofana muzitshita. Ndimo anaitana kwa ie antu ambiri
15 inso, nanena nao, Imvani ine inu nonse, ndi dziwani: kulibe
kantu kwa kunja kwa muntu, komwe kamloa kadziwa
kumdetsa: koma zintu zomwe zituruka mwa muntu ziri
17 zomwe zidetsa muntu. Ndimo ntawi analoa m' nyumba kwa
18 antu ambiri, akupunzira atshi namfunsa ndi fanizo. Ndimo
anena nao, Kodi muli tshointsho opanda nzeru uuso?
Musadziwitsa, kuti tshintu tshomwe tshakunja tshiloa m'
19 muntu, tshosadziwa ku detsa ie; tshifuka tshosaloa muntima
mwatshi, koma m' mimba mwatshi, ndimo tshituruka m'

poonyera? *Tshimene nanena*, kupanga kudia konse kutsuka.
Ndimo nati, Tshimene tshomwe tshituruka mwa muntu, 20
tshomwe tshidetsa muntu. Kuti mwa umo, mwa ntima wa 21
antu, maganizo oipa zituruka, madama, zimbala, ambanda, 22
zigololo, malisirira, zimpulupulu, tshinyengo, kufuna tshigo-
lolo, diso loipa, kutukwana, kudzitama, kupusa: zintu 23
zonse zimene zoipa zituruka mwa umo, nazidetsa muntu.

Ndimo apo nauka, nang'ka ku maliri a Tire ndi Tsidon. 24
Naloa m' nyumba, ndimo sanafuna muntu modzi ku dziwa:
ndimo sanadziwa ku bisidwa. Koma tsopano lino nkazi, 25
kabutu ka emwe kanali ndi nzimu wosatsuka, anamva ndi
ie, nadza nagwa pa mapazi atshi. Ndimo nkazi anali 26
Mgrike, Msirofenisi ndi fuko. Ndimo nampempa kuti
akaturutse demon mwa kabutu katshi. Ndimo nanena nai', 27
Ana akute patsogolo: kuti sitshiri tshabwino ku tenga nkate
wa ana, ndi kuutaia kwa agaru. Koma naiang'ka ndimo 28
anena nai', Inde, Mwini: inde agaru pansi pa gome adia
nyenyeswa za ana. Ndimo nanena nai', Kwa kunena 29
kumene muka; demon waturuka mwa kabutu kako. Ndimo 30
napita ku nyumba yatshi, napeza kamwana kaikidwa pa
kama, ndi demon waturuka.

Ndimo onso namuka ku maliri a Tire, nafika mwa Tsidon 31
ku nyanja ya Galileya, pakati pa maliri a Dekapolis. Ndimo 32
atenga kwa ie modzi emwe anali wogonta, ndimo anali ndi
matutu; ndimo ampempa ku ika dzanja latshi pa ie.
Ndimo namtenga kwa antu ambiri kutseri, naika dzala 33
dzatshi m' makutu atshi, nalabvula mate, natosa lilume
latshi; ndimo kuyang'ana ku mwamba, napuma tuntuli, 34
ndimo anena nai', Efata, omwe ali, Tsegudwani. Ndimo 35
makutu atshi anatsegudwa, ndi tshingwe tsha lilume latshi
tshinamasulidwa, ndimo nalankula bwino. Ndimo nauza 36
awo kuti sakanena ndi muntu: koma nauza awo kwambiri,
kopambana awa anabukitsa. Ndimo nazizwa kosayeza, 37
kuti, Watshita zintu zonse bwino: apanga inde agonti ku
mva, ndi osalankula ku lankula.

M' masiku adya, ntawi anali inso antu ambiri, ndimo 8
alibe kantu ku dia, naitana kwa ie akupunzira atshi, ndimo
anena nao, Diri ndi tshisoni ndi antu ambiri, tshifuka 2
tsopano akalabe ndi ine masiku atatu, ndimo alibe kantu
ku dia: ndimo ngati ditshotsa awa ndi njala kwao, adzafoka 3
pa njira; ndi ena a awa anadzera kutali. Ndimo akupu- 4
nzira atshi namwiang'ka, Kuti modzi adzadziwa ku kutitsa

antu amene ndi mikate muno m' tshipululu? Ndimo
5 nafunsa awa, Muli ndi mikate ingati? Ndimo anati, Isanu
6 ndi iwiri. Ndimo auza antu ambiri ku kala pansi: natenga
mikate isanu ndi iwiri, nati tshakoma, naswa, napatsa ku
akupunzira atshi, ku ika patsogolo pa awo; ndimo naiika
7 patsogolo pa antu ambiri. Ndimo anali nazo nsomba
zazing'ono zowereng'jeka: ndimo anadalitsa izo, nauza
8 kuziika anso patsogolo pa awo. Ndimo anadia, nakuta:
ndimo natola, za nyenyeswa zomwe zinatsala, mitanga
9 isanu ndi iwiri. Ndimo anali kwa mazousan anai: ndimo
10 natshotsa awa. Ndimo tsopano lino naloa m' tshombo ndi
akupunzira atshi, nadza kwa maliri a Dalmanuta.
11 Ndimo Afarisi anaturuka, naamba ku funsa ie, kufuna
12 kwa ie tshizindikilo kwa kumwamba, kuyesa ie. Ndimo
napuma tuntuli kolimba m' nzimu watshi, ndimo ati, Fuko
limeneli lifuna tshizindikilo bwanje? dinena ndi inu nditu,
Tshizindikilo palibe tshidzapatsidwa ku fuko limeneli.
13 Ndimo nasia awa, ndi kuloa anso m' *tshombo* namuka
kutsidia lina.
14 Ndimo anaiwala ku tenga nkate; ndimo osali nao m'
15 tshombo wopambana nkate umodzi. Ndimo nauza awo,
kuti, Yang'anani, tshenjerani ndi fumba ya Afarisi ndi
16 fumba ya Herode. Ndimo nasing'kasing'ka modzi ndi wina,
17 kuti, Tiribe nkate. Ndimo Yesu kudziwitsa anena nao,
Musing'kasing'ka bwanje, tshifuka mulibe nkate? kodi
simudziwitsa kosuntira, kapena simudziwa? kodi muli ndi
18 mitima yanu yolimbikitsidwa? Kupotshera maso, simuona?
ndi kupotshera makutu, simumva? ndi simukumbukila?
19 Ntawi dinaswa mikate isanu mwa mazousan asanu, mitanga
ingati yodzaza ndi zinyenyeswa munatola? Anena nai',
20 Kumi ndi iwiri. Ndimo ntawi isanu ndi iwiri mwa mazousan
anai, mitanga ingati yodzaza ndi zinyenyeswa munatola?
21 Ndimo anena nai', Isanu ndi iwiri. Nanena nao, Kodi
simudziwa kosuntira?
22 Ndimo adza ku Betsayida. Ndimo atenga kwa ie
23 mamuna wakungu, napempa ie kumtosa. Ndimo natenga
mamuna wakungu ndi dzanja, naturuka nai' m' mudzi;
ndimo ntawi nalabvula mate pa maso atshi, ndimo anaika
24 manja atshi pa ie, namfunsa, Kodi uona kantu? Ndimo
nayang'ana ku mwamba, nati, Diona antu; kuti diona *awa*
25 monga mitengo, kuendaenda. Pomwe enso naika manja
atshi pa maso atshi; nayang'anitsa, natshiritswa, naona

bwino zintu zonse. Ndimo, namtumiza kwatshi, kuti, 26
Usaloa inde m' mudzi.
Ndimo Yesu naturuka, ndi akupunzira atshi, ku midzi ya 27
Kesareya wa Filipu: ndimo pa njira nafunsa akupunzira
atshi, kunena nao, Antu anena kuti diri ani? Ndimo 28
nauza ie, kuti, Yohane Mbapatizi: ndi ena, Eliya; koma
ena, Modzi wa Aprofeti. Ndimo nafunsa awo, Koma 29
munena kuti diri ani? Petros aiang'ka ndimo anena nai',
Uli Kristu. Nauza awa kuti akanena palibe muntu ndi 30
ie. Ndimo naamba ku punzitsa awa, kuti Mwana wa 31
muntu akanamva zintu zambiri, nakanidwa ndi akuru, ndi
adzukuru akuru, ndi akulembera, ndi apedwa, ndi pambuiu
masiku atatu auka anso. Nalankula mau poyera. Ndimo 32
Petros namtenga, naamba ku sulumula ie. Koma ie kute- 33
mbenuka, ndi kuona akupunzira atshi, anasulumula Petros,
ndimo ati, Pita kumbuiu kwa ine, Satana: kuti usasamala
zintu za Mulungu, koma zintu za antu. Ndimo naitana 34
kwa ie antu ambiri ndi akupunzira atshi, nanena nao,
Ngati muntu modzi afuna kunditsata, adzikanize, natukule
nkhwitshi yatshi, nanditsate. Kuti iemwe afuna ku pulu- 35
mutsa moyo watshi adzaumwaza; ndimo iemwe adzamwaza
moyo watshi kwa ine ndi kwa ivangeli adzaupulumutsa.
Kuti ninje tshipindula muntu, ku lemerera dziko lonse, 36
namwaza moyo watshi? Kuti ninje muntu akasinta kwa 37
moyo watshi? Kuti iemwe adzakala ndi manyazi ndi ine 38
ndi mau anga mwa fukolimeneli latshigololo ndi lampulupulu,
Mwana wa muntu unso adzakala ndi manyazi ndi ie, ntawi
adza mwa kupambana kwa Atatu atshi ndi anjelo oyera.
Ndimo nanena nao, Dinena ndi inu nditu, Alipo ena a awa 9
omwe aima *pano*, omwe sadzalawa imfa nditu, kwa ntawi
aona dziko la Mulungu lidza ndi mpamvu.
Ndimo pambuiu masiku asanu ndi limodzi Yesu atenga 2
ndi ie Petros, ndi Yakobi, ndi Yohane, ndimo atsogolera
awa pa piri lalitali iwo oka kutseri: nasandulizidwa patso-
golo pa awo: ndimo miinjiro yatshi inakala yowala, yoyera 3
kwambiri; tshointsho monga palibe wotsuka pansi pano
adziwa ku yeretsa iyo. Ndimo kunaonekera ku awo Eliya 4
ndi Moses: ndimo analikulankulana ndi Yesu. Ndimo 5
Petros aiang'ka nanena ndi Yesu, Rabi, tshiri tshabwino
kwa ife tiri pano: ndimo timange misasa itatu; limodzi
kwa iwe, ndi limodzi kwa Moses, ndi limodzi kwa Eliya.
Kuti sanadziwa tshiani ku yang'ka; kuti naopa kwambiri. 6

7 Ndimo kunafika ntambo kupimba awo: ndimo linaturuka
liu muntambo, Amene ali Mwana wanga wondikonda:
8 imvani ie. Ndimo nsanga kuyang'anayang'ana, naona palibe
modzi inso, koma Yesu eka ndi awo oka.
9 Ndimo monga analikutsika ku piri, nauza awo kuti
sakauza muntu modzi zintu zomwe anaziona, koma ntawi
10 Mwana wa muntu akanauka anso kwa akufa. Ndimo
nasunga mau, kufunsana ninje kuuka anso kwa akufa kuta-
11 ntauza. Ndimo namfunsa, kuti, Akulembera anena kuti
12 Eliya akanadza kwiamba. Ndimo nanena nao, Eliya adza
pakwiamba nditu, nafotokoza zintu zonse: nanga bwanje
tshilembedwa ndi Mwana wa muntu, kuti akamva zintu
13 zambiri nakatonzedwa? Koma dinena ndi inu, kuti Eliya
wadza, ndimo anatshita anso kwa ie zomwe anazifuna, inde
monga tshilembedwa ndi ie.
14 Ndimo ntawi nadza ku akupunzira, naona antu ambiri
15 ozungulira awa, ndi akulembera kufunsira awa. Ndimo
tsopano lino antu ambiri onse, ntawi anamona, nazizwa
16 kwambiri, ndimo kutamanga kwa ie nautsa ie. Ndimo
17 nafunsa awo, Mufunsira tshiani ndi awa? Ndimo modzi wa
antu ambiri naiang'ka ie, Mpunzitsi, datengera kwa iwe
mwana wanga, emwe ali ndi nzimu wosadziwa ku lankula:
18 ndimo pomwe umtengera, numkung'khuniza: ndimo akala
ndi pobvu, nakukuta mano atshi, naonda: ndimo danena
ndi akupunzira ako monga kuti akauturutsa; ndimo sana-
19 dziwa. Ndimo aiang'ka awa, nati, O fuko losamvana,
ntawi ingati didzakala ndi inu? ntawi ingati didzalekereza
20 inu? tengani ie kwa ine. Ndimo namtenga kwa ie: ndimo
ntawi namona, tsopano lino nzimu wampweteketsa kwa-
mbiri; nagwa pansi, nakung'khunika nakala ndi pobvu.
21 Ndimo nafunsa atatu atshi, Ntawi yapita bwanje kumene
22 kunadza kwa ie? Nati, Ntawi anali mwana. Ndimo
ntawi zambiri unamponya m' moto ndi m' madzi, kummwa-
za: koma ngati udziwa ku tshita kantu, kala ndi tshisoni
23 ndi ife, nutitangata. Ndimo Yesu nanena nai', Ngati
24 udziwa! Zintu zonse ziteka kwa iemwe amvana. Tsopano
lino atatu atshi a mwana napfula, nanena, Dimvana;
25 utangate kusamvana kwanga. Ndimo ntawi Yesu naona
kuti antu ambiri natamanga pa modzi, nasulumula
nzimu wosatsuka, kunena ndi iwo, Nzimu wosadziwa ku
lankula ndi wogonta, dikuuza, turuka mwa ie, nusaloa anso
26 mwa ie. Ndimo unapfula, numpweteketsa kwambiri,

nuturuka: ndimo *mwana* anakala monga modzi wafa; monga
kuti unyinji unanena, Wafa. Koma Yesu namtenga ndi 27
dzanja, namtukula; ndimo nauka. Ndimo ntawi analoa 28
m' nyumba akupunzira atshi namfunsa kutseri, *kuti*, Sitina-
dziwa kuuturutsa. Ndimo nanena nao, Fuko limene losa- 29
dziwa ku turuka ndi kantu kena, koma ndi kupempera.

Ndimo anatshoka apo, napita mwa Galileya; ndimo 30
sanafuna kuti muntu modzi akadziwa. Kuti napunzitsa 31
akupunzira atshi, nanena nao, Mwana wa muntu aperekedwa
ku manja a antu, ndimo adzampa; ndimo ntawi apedwa,
pambuiu masiku atatu adzauka anso. Koma sanadziwa 32
mau, naopa kumfunsa.

Ndimo nafika ku Kapernahum: ndimo ntawi anali m' 33
nyumba nafuusa awa, Munaweruzana tshiani m' njira?
Koma anatontola: kuti anakangana modzi ndi wina m' njira, 34
wang'kuru wopambana *anali* ndani. Ndimo nakala pansi, 35
naitana kumi ndi awiri; ndimo anena nao, Ngati muntu
modzi afuna ku kala patsogolo, ie adzakala pambuiu pa
onse, ndi woimirira wa onse. Ndimo natenga kamwana, 36
nakaika pakati pa awo: ndimo kukaangata, nanena nao,
Iemwe adzalandira kamodzi ka tiana totere m' dzina langa, 37
alandira ine: ndi iemwe alandira ine, wosalandira ine, koma
iemwe ananditumiza.

Yohane naiang'ka ie, Mpunzitsi, tinaona modzi kuturutsa 38
ademon m' dzina lako: ndimo tinamletsa, tshifuka sanatitsata.
Koma Yesu wati, Musamletsa: kuti palibe muntu emwe 39
adzatshita mpamvu m' dzina langa, ndimo adziwa nsanga ku
nena zoipa ndi ine. Kuti emwe wosali pa ife ali kwa ife. 40
Kuti emwe adzakupatsani tshiko tsha madzi ku mwa, tshi- 41
fuka muli a Kristu, dinena ndi inu nditu, sadzataia sekeretso
latshi nditu. Ndimo emwe adzakwiitsa modzi wa tating'ono 42
timene tomwe timvana ndi ine, kuli bwino kwa ie ngati
mpero yeikuru inamangidwa pa kosi latshi, naponyedwa m'
nyanja. Ndimo ngati dzanja lako likukwiitsa, dula: kuli 43
bwino kwa iwe ku loa m' moyo watshipunumbu, kopambana
kukala ndi manja ako awiri ku loa m' geena, m' moto wosa-
zimika. Ndimo ngati pazi lako likukwiitsa, dula: kuli 45
bwino kwa iwe ku loa m' moyo watshipunumbu, kopambana
kukala ndi mapazi ako awiri ku ponyedwa m' geena.
Ndimo ngati diso lako likukwiitsa, konombola ilo: kuli 47
bwino kwa iwe ku loa m' dziko la Mulungu ndi diso li-
modzi, kopambana kukala ndi maso awiri ku ponyedwa m'

48 geena; pomwe nyongolotsi yao yosafa, ndi moto wosazi-
49 midwa. Kuti onse adzapakidwa ndi ntshere wa moto.
50 Ntshere uli wabwino: koma ngati ntshere unataika nyongo
yatshi, udzakometsa iwo ndi tshiani? Potsherani ntshere
mwa inu noka, ndi kalani ndi ntendere modzi ndi wina.

10 Ndimo nauka uko, ndimo adza m' maliri a Yudeya ndi
patsidia lina la Yordan: ndi antu ambiri asong'kana anso
kwa ie: ndimo, monga anazolowera, napunzitsa awa anso.
2 Ndimo nadza kwa ie Afarisi, namfunsa, Kodi tshiri tshamau
3 kwa muntu ku tshotsa nkazi *watshi?* kuyesa ie. Naiang'ka
4 nanena nao, Moses nakuuzani bwanje? Ndimo anati, Moses
nalola ku lemba nkalata wa kulekana, ndimo kumtshotsa.
5 Koma Yesu nanena nao, Kwa kulimbika kwanu kwa mitima
6 nalembera inu mau amene. Koma kwa kwiamba kwa
7 kupanga, Wamamuna ndi wankazi napanga awo. Kwa
tshifukwa tshimene muntu adzasia atatu atshi ndi amai atshi,
8 nadzagwirizana ndi nkazi watshi; ndimo awiri adzakala
nyama imodzi: monga kuti palibe awiri inso, koma nyama
9 imodzi. Ndimo tshomwe Mulungu anapatikiza, muntu
10 aleke ku lekanitsa. Ndimo m' nyumba akupunzira namfunsa
11 anso ndi tshimenetshi. Ndimo anena nao, Iemwe adzaleka
12 nkazi watshi, nakwata wina, atshita tshigololo pa ie: ndimo
ngati ie eka adzaleka mamuna watshi, nakwatidwa ndi wina,
atshita tshigololo.
13 Ndimo natenga kwa ie tiana tating'ono, kuti akatitose:
14 ndi akupunzira nasulumula awo. Koma ntawi Yesu naona,
nakwia, nanena nao, Lekani tiana ku dza kwa ine; musati-
15 letsa: kuti ndi totere liri dziko la Mulungu. Dinena ndi
inu nditu, Iemwe sadzalandira dziko la Mulungu monga
16 kamwana, sadzaloa umo nditu. Ndimo anatiangata, natida-
litsa, kuika manja atshi pa ito.
17 Ndimo monga analikupita pa njira, natamanga modzi kwa
ie, nagwada kwa ie, namfunsa, Mpunzitsi wabwino, didza-
18 tshita tshiani kuti diloe moyo wosamariza? Ndimo Yesu
nanena nai', Utsha ine wabwino bwanje? palibe modzi
19 wabwino koma modzi, *inde* Mulungu. Udziwa mau, Usapa,
Usatshita tshigololo, Usaba, Usasinjirira, Usanyenga, Leme-
20 keza atatu ako ndi amai ako. Ndimo nanena nai', Mpunzitsi,
21 zintu zonse zimenezi dinasunga kwa ubwana wanga. Ndimo
Yesu kumyang'ana namkonda, nanena nai', Tshintu tshimodzi
usoa: muka, gulitsa zomwe uli nazo, nupatsa kwa osauka, ndimo
udzapotshera kulemera m' mwamba: ndimo nudza, nundi-

tsata. Koma nkope yatshi inagwa pa mau, ndimo namuka ndi 22
tshisoni: kuti anali modzi emwe anali ndi mapotshero akuru.
Ndimo Yesu nayang'anayang'ana, ndimo anena ndi 23
akupunzira atshi, Bwanje awa omwe ali ndi zolemera
adzaloa koserera m' dziko la Mulungu! Ndimo akupunzira 24
nazizwa ndi mau atshi. Koma Yesu aiang'ka anso, nanena
nao, Ana, kuserera kuli bwanje ku awa omwe amvana ndi
zolemera ku loa m' dziko la Mulungu! Kuli kopepuka 25
kwa gamila ku pisa mpanda ya kasingano, kopambana ndi
kwa muntu wolemera ku loa m' dziko la Mulungu. Nazi- 26
zwa kwambiri, kunena nai', Pomwe ndani adziwa ku pulu-
mutsidwa? Yesu kuyang'ana pa iwo ati, Ndi antu tshiri 27
tshosateka, koma iai ndi Mulungu: kuti zintu zonse ziteka
ndi Mulungu. Petros naamba ku nena nai', Ona, tasia 28
zonse, ndimo takutsata. Yesu nanena, Dinena ndi inu 29
nditu, Palibe muntu emwe anasia nyumba, kapena abali, kape-
na alongo *atshi*, kapena amai *atshi*, kapena atatu *atshi*, kapena
ana, kapena minda, kwa ine, ndi kwa ivangeli, koma adza- 30
landira makumi okaoka kumi limodzi tsopano m' ntawi
imene, zinyumba, ndi abali, ndi alongo *atshi*, ndi amai *atshi*,
ndi ana, ndi minda, ndi zinkarwe; ndimo m' kugonera ku
dza moyo wosamariza. Koma ambiri *omwe ali* apatsogolo 31
adzakala apambuiu; ndi apambuiu apatsogolo.
Ndimo anali pa njira, kukwera ku Yerusalem; ndi Yesu 32
analikupita patsogolo pa awo: ndimo nazizwa; ndimo awo
omwe natsata naopa. Ndimo natenga anso kumi ndi awiri,
naamba ku uza awa zintu zomwe zirinkudza kwa ie, *kuti*, 33
Ona, tikwera ku Yerusalem; ndimo Mwana wa muntu adza-
perekedwa kwa adzukuru akuru ndi kwa akulembera;
ndimo adzasutsa ie kwa imfa, nadzapereka ie kwa Mitundu:
ndimo adzatonza ie nadzalabvula mate pa ie, nadzakwapula 34
ie, nadzapa ie; ndimo pambuiu masiku atatu adzauka anso.
Ndimo ayandika ie Yakobi ndi Yohane, ana a Zebediya, 35
kunena nai', Mpunzitsi, tifuna kuti ukatshitira ife tshomwe
tidzatshipempa iwe. Ndimo nanena nao, Mufuna tshiani 36
kuti dikatshitira inu? Ndimo ananena nai', Bvomereza ife 37
kuti tikale, modzi pa dzanja lako lamanja, ndi wina pa
dzanja *lako* lamanzere, m' kupambana kwako. Koma Yesu 38
nanena nao, Musadziwa tshomwe mupempa: Kodi mudziwa
ku mwa ndi tshiko tshomwe dimwera? kapena ku bapa-
tizidwa ndi mbapatisma lomwe dibapatiziridwa? Ndimo 39
nanena nai', Tidziwa. Ndimo Yesu nanena nao, Tshiko

tshomwe dimwera mudzamwera; ndimo ndi mbapatisma
40 lomwe dibapatizidwa mudzabapatizidwa: koma ku kala
pa dzanja langa lamanja kapena pa dzanja *langa* lama-
nzere si kuli kwanga ku patsa: koma *kuli kwa awo* kwa
41 omwe kwakonzetsedwa. Ndimo ntawi kumi anamva,
42 naamba ku kwiira ndi Yakobi ndi Yohane. Ndimo Yesu
anaitana awo kwa ie, nanena nao, Mudziwa kuti omwe
aganizidwa ku weruza Mitundu aweruza iyo; ndi akuru ao
43 atshita mpamvu pa iyo. Koma sitshiri tshointshi mwa inu:
koma iemwe afuna ku kala wang'kuru mwa inu, adzakala
44 woimirira wanu: ndi iemwe afuna ku kala wapatsogolo
45 mwa inu, adzakala kapolo wa onse. Kuti nditu Mwana wa
muntu sanafika ku imiriridwa, koma ku imirira, ndi ku
patsa moyo watshi dombolo kwa ambiri.
46 Ndimo afika ku Yeriko: ndimo monga naturuka ku
Yeriko, ndi akupunzira atshi ndi antu ambiri, mwana wa
Timeyu, Bartimeyu, wopempa wakungu, analikukala mbali
47 mwa njira. Ndimo ntawi anamva kuti anali Yesu wa
Nazarete, naamba ku pfula, nati, Yesu, mwana wa Davide,
48 kala ndi nsisi ndi ine. Ndimo ambiri nasulumula ie, kuti
atontole: koma napfula kolimbika kopambana, Mwana wa
49 Davide, kala ndi nsisi ndi ine. Ndimo Yesu naima, nanena,
Mwitana ie. Ndimo aitana muntu wakungu, kunena nai',
50 Kala wosekera: uka, akuitana. Ndimo ie, kutaia mwinjiro
51 watshi, nauka nsanga, nadza kwa Yesu. Ndimo Yesu
naiang'ka ie, nati, Ufuna tshiani tshomwe ditshita ndi iwe?
Ndimo muntu wakungu nanena nai,' Raboni, kuti dilandire
52 kuona kwanga. Ndimo Yesu nanena nai', Muka; mvanu
wako watshiritsa iwe. Ndimo tsopano lino nalandira kuona
kwatshi, natsata ie m' njira.
11 Ndimo ntawi ayandika kwa Yerusalem, kwa Betefage ndi
Betaniya, pa piri la Maolive, atumiza awiri a akupunzira
2 atshi, nanena nao, Mukani m' mudzi womwe uli pandunji pa
inu: ndimo tsopano lino monga muloa momwe, mudzapeza
mwana wa buru womangidwa, pomwe palibe muntu anakala
3 ntawi yapita: masulani ie, ndimo mutenga ie. Ndimo
ngati modzi anena ndi inu, Mutshita bwanje tshimenetshi?
nenani, Mwini ali ndi kufunidwa ndi ie: ndimo tsopano
4 lino adzamtumiza kuno. Ndimo namuka, napeza mwana
wa buru womangidwa pa tshitseko kunja pa kwalala; ndimo
5 amasula ie. Ndimo ena a awo omwe naima apo nanena
6 nao, Mutshita tshiani, kumasula mwana wa buru? Ndimo

nanena nao inde monga Yesu ananena: ndimo nabvomera.
Ndimo atenga mwana wa buru kwa Yesu, naika pa ie 7
miinjiro yao; ndimo nakala pa ie. Ndimo ambiri nayala 8
miinjiro yao pa njira; ndi ena matsatsa, omwe anadula kwa
minda. Ndimo awo omwe anapita patsogolo, ndi omwe 9
anatsata, napfula, Hosana; Wodala *ali* emwe adza m' dzina
la Mwini: Lodala *liri* dziko lomwe lidza, *dziko la* atatu atu 10
Davide: Hosana mopambanitsa.

Ndimo naloa m' Yerusalem, m' tempile; ndimo ntawi 11
anayang'anayang'ana pa zintu zonse, tsopano madzulo,
naturuka kwa Betaniya ndi kumi ndi awiri.

Ndimo pa mawa ntawi anadzera kwa Betaniya, anamva 12
njala. Ndimo kuona nkuyu kutali unali ndi masamba, 13
nafika, ngati kapena anangopeza kantu pa iwo: ndimo
ntawi nafika kwa iwo, napeza palibe kantu koma masamba;
kuti siinali ntawi ya zinkhuyu. Ndimo naiang'ka nanena 14
nao, Palibe muntu adie dzobala kwa iwe kwa ntawi
imene kwa ntawi zonse. Ndimo akupunzira atshi
anamva.

Ndimo adza kwa Yerusalem: ndimo naloa m' tempile, 15
naamba ku turutsa awo omwe nagulitsa ndi awo omwe
nagula m' tempile, natembenuza magome a akusintana
ndrama, ndi mipando ya awo omwe nagulitsa zinjiwa;
ndimo sanaleka kuti muntu modzi akanyamula tshiwira 16
pandule pa tempile. Ndimo napunzitsa, nanena nao, Kodi 17
sikulembedwa, Nyumba yanga idzatshedwa nyumba ya
kupempera kwa mitundu yonse? koma munaipanga panga
la olanda. Ndimo adzukuru akuru ndi akulembera anamva, 18
nafuna bwanje anangomwaza: kuti namopa, kuti antu
ambiri onse nazizwa ndi kupunzitsa kwatshi.

Ndimo madzulo onse naturuka muzinda. 19

Ndimo monga napita mamawa, naona nkuyu wouma kwa 20
mitsitsi. Ndimo Petros alikukumbukila anena nai', Rabi, 21
ona, nkuyu womwe unautonza wapakatika. Ndimo Yesu 22
kuiang'ka anena nao, Potsherani mvanu ndi Mulungu.
Dinena ndi inu nditu, Emwe adzanena ndi piri limene, 23
Tukulidwa nuponyedwa m' nyanja; ndimo sadzakaikiza
muntima mwatshi, koma adzamvana kuti tshomwe anena
tshidzakala; adzatshipotshera. Ndimo dinena ndi inu, 24
Zintu zonse zomwe mupempera ndi mufunsira, mvanani
kuti mwalandira izo, ndimo mudzapotshera izo. Ndimo 25
ntawi yomwe muima kupempera, kululukirani, ngati muli

ndi kantu pa modzi; kuti Atatu anu unso emwe ali m'
mwamba, angokululukira inu matshimo anu.
27 Ndimo adza anso ku Yerusalem: ndimo monga analiku-
endaenda m' tempile, adza kwa ie adzukuru akuru, ndi
28 akulembera, ndi akuru; ndimo nanena nai', Ndi mpamvu
yanje utshita zintu zimenezi? kapena wakupatsa mpamvu
29 imene ndani ku tshita zintu zimenezi? Ndimo Yesu
nanena nao, Didzafunsa inu mau amodzi, ndimo yang'kani
ine, ndimo didzakuuzani ndi mpamvu yanje ditshita zintu
30 zimenezi. Mbapatisma la Yohane, kodi linali kwa kumwa-
31 mba, kapena kwa antu? yang'kani ine. Ndimo nasing'ka-
sing'ka iwo oka, kuti, Ngati tidzanena, Kwa kumwamba;
32 adzati, Nanga bwanje musanamvana ndi ie? Koma ngati
tikati, Kwa antu—anaopa antu: kuti onse anaganiza nditu
33 Yohane anali mprofeti. Ndimo naiang'ka Yesu ndimo
anena, Sitidziwa. Ndimo Yesu anena nao, Kapena si-
ndikuuzani ndi mpamvu yanje ditshita zintu zimenezi.
12 Ndimo naamba ku nena nao ndi mafanizo. Muntu
naoka munda wa mvina, naika tshinga kozungulira uo,
nakumbira tshiwira tsha vinyo, namanga sanja, naubwereka
2 kwa otshita munda, nang'ka ku dziko lina. Ndimo pa
nsiku natumiza ku otshita munda kapolo, kuti anangolandira
kwa otshita munda ndi dzobala dza munda wa mvina.
3,4 Ndimo namgwira, nammenya, namtumiza tshabe. Ndimo
onso natumiza kwa awo kapolo wina; ndimo ie namlasa
5 mutu, ndimo nampyapyaza. Ndimo natumiza wina; ndimo
ie anampa: ndi ambiri ena; kumenya ena, ndi kupa ena.
6 Anali ndi modzi kosuntira, mwana wokondedwa: natumiza
ie patungo ku awo, kuti, Adzalemekeza mwana wanga.
7 Koma otshita munda amenewo nauzana, Amene ali woloa;
8 tieni, timpe, ndimo tsholoa tshidzakala tshatu. Ndimo na-
9 mgwira, nampa, namturutsa m' munda wa mvina. Ndimo
mwini wa munda wa mvina adzatshita tshiani? adzafika
nadzamwaza otshita munda, ndimo adzapatsa munda wa
10 mvina kwa ena. Kodi simunawerenga inde lemba limene;
Mwala womwe omanga naukana,
Womwe unapangidwa mutu wa ngondia:
11 Tshimene tshinali kwa Mwini,
Ndimo tshiri tshozizwa m' maso atu?
12 Ndimo nafuna kumgwira; ndimo naopa antu ambiri; kuti
nadziwitsa kuti nanena fanizo pa awo: ndimo anamleka,
namuka.

Ndimo atumiza kwa ie ena a Afarisi ndi a Aherode, kuti 13
anangomkola m' mau. Ndimo ntawi anadza, anena nai', 14
Mpunzitsi, tidziwa kuti uli wanteradi, ndimo usasamala
modzi: kuti usayang'ana makalidwe a antu, koma mwa
nteradi upunzitsa njira ya Mulungu: Kodi tshiri tshamau
ku patsa tsong'ko ku Kesare, kapena iai? Kodi tipatsa, 15
kapena sitipatsa? Koma ie, kudziwa tshinyengo tshao,
nanena nao, Muyesa ine bwanje? tengani denariyon, kuti
dilione. Ndimo nalitenga. Ndimo anena nao, Kufaniza 16
kumene ndi kulemba ziri za ani? Ndimo nanena nai',
Za Kesare. Ndimo Yesu nanena nao, Perekani kwa Kesare 17
zintu zomwe ziri za Kesare, ndi kwa Mulungu zintu zomwe
ziri za Mulungu. Ndimo nazizwa kwambiri ndi ie.

Ndimo adza kwa ie Asadusi, omwe anena kuukirira 18
palibe: ndimo namfunsa, kuti, Mpunzitsi, Moses nalembera 19
ife, Ngati njiratshi wa muntu afe, nasia nkazi pambuiu pa
ie, nasia wopanda ana, kuti mpwatshi akatenga nkazi watshi,
ndimo akaukitsa mbeu kwa njiratshi. Kunali abali ao 20
asanu ndi awiri: ndimo woiamba natenga nkazi, nafa, nasia
palibe mbeu; ndimo watshiwiri namtenga, nafa, kusia 21
palibe mbeu; ndi watshitatu modzimodzi: ndimo asanu ndi 22
awiri anasia palibe mbeu. Pambuiu pa onse nkazi nafa
anso. Mwa kuukirira nkazi wa ani adzakala wa awo? kuti 23
asanu ndi awiri anapotshera ie, nkazi. Yesu nanena nao, 24
Kodi sikuli kwa tshifukwa tshimene kodi musotshera, kuti
musadziwa malemba, kapena mpamvu ya Mulungu? Kuti 25
ntawi adzauka kwa akufa, kapena osakwata, kapena osapa-
tsidwa ku kwatibwa; koma akala monga anjelo m' mwamba.
Koma ndi akufa, kuti aukitswa; kodi simunawerenga m' 26
buku la Moses, *m' malo ndi* Tshifutu, bwanje Mulungu
nanena nai', kuti, Di*ri* Mulungu wa Abraham, ndi Mulungu
wa Yisake, ndi Mulungu wa Yakobi? Wosali Mulungu 27
wa akufa, koma wa amoyo: musotshera kwambiri.

Ndimo modzi wa akulembera nadza, namva awo kufunsa- 28
na, ndimo kudziwa kuti anaiang'ka awa bwino, namfunsa,
Tshiani tshiri mau tshopambana pa onse? Yesu naiang'ka, 29
Tshopambana tshiri, Imva, O Sirayeli; Mwini Mulungu
watu, Mwini ali modzi: ndimo udzakonda Mwini Mulungu 30
wako ndi ntima wako wonse, ndimo ndi nzimu wako wonse,
ndimo ndi muwongo wako wonse, ndimo ndi mpamvu yako
yonse. Ndi atshiwiri ali amene, Udzakonda woiandikila 31
wako monga iwe eka. Palibe mau ena opambana amenewa.

32 Ndimo wolembera nanena nai', Wa nteradi, Mpunzitsi,
wanena bwino kuti ie ali modzi; ndimo palibe wina koma
33 ie: ndimo ku konda ie ndi ntima wonse, ndi kudziwa
konse, ndi mpamvu yonse, ndi ku konda woiandikila watshi
monga ie eka, kuli kwambiri kopambana nsembe zootsha
34 zatuntu zonse, ndi zinsembe. Ndimo ntawi Yesu naona
kuti anaiang'ka ndi nzeru, nanena nai', Suli kutali ndi
dziko la Mulungu. Ndimo palibe muntu pambuiu pamene
nayesa kumfunsa funso lina.

35 Ndimo Yesu naiang'ka nanena, monga napunzitsa m'
tempile, Akulembera ati bwanje kuti Kristu ali mwana wa
36 Davide? Davide eka nanena m' Nzimu Woyera,

Mwini nanena ndi Mwini wanga,
Kala iwe pa dzanja langa lamanja,
Kwa ntawi dipanga maliwongo ako mpando wa mapazi
ako.

37 Davide eka atsha ie Mwini; ndimo kuti ali mwana watshi?
Ndimo antu atshabe anamva ie kosekera.

38 Ndimo m' kupunzitsa kwatshi nanena, Tshenjerani ndi
akulembera, omwe afuna ku enda m' miinjiro yeitali, ndi
39 *ku potshera* mautso m' malo a maronda, ndi mipando yeikuru
40 m' masinagoge, ndi malo akuru pa kudia: awo omwe
aononga nyumba za amasie, ndimo kwa tshinyengo apanga
mapempero atali; amene adzalandira kusutsa kwakukuru.

41 Ndimo nakala pansi pandunji pa bokosi la ndrama, naona
bwanje antu ambiri naika ndrama m' bokosi la ndrama:
42 ndimo ambiri omwe anali olemera naika zambiri. Ndimo
nadza wamasie modzi wosauka, ndimo naika timite tiwiri,
43 tomwe tipanga fardin limodzi. Ndimo naitana kwa ie
akupunzira atshi, nanena nao, Dinena ndi inu nditu,
Wamasie wosauka amene anaika kopambana onse omwe
44 alikuika m' bokosi la ndrama: kuti awo onse naika kwa
zambiri zao; koma ie kwa kusauka kwatshi naika zonse
zomwe anali nazo, *inde* moyo watshi wonse.

13 Ndimo monga analikuturuka m' tempile, modzi wa aku-
punzira atshi anena nai', Mpunzitsi, ona, miala yanje ndi
2 zomangidwa zanje! Ndimo Yesu nanena nai', Kodi uona
zomangidwa zimene zazikuru? palibe udzatsala pano mwala
umodzi pa wina, womwe wosadzaponyedwa.

3 Ndimo monga nakala pansi pa piri la Maolive pandunji pa
tempile, Petros ndi Yakobi ndi Yohane ndi Andreya nafunsa
4 ie kutseri, Uza ife, ntawi iti zintu zimenezi zidzakala? ndimo

tshiani *tshidzakala* tshizindikilo ntawi zıntu zonse zimenezi
zirikufuna ku tedwa? Ndimo Yesu naamba ku nena nao, 5
Tshenjerani kuti palibe muntu adzasotshereza inu. Ambiri 6
adzafika m' dzina langa, kuti, Diri *ie:* ndimo adzasotshereza
ambiri. Ndimo ntawi mudzamva ndi zinkondo ndi mbiri 7
za zinkondo, musatuntumiridwa: *zintu zimenezi* zikanakala;
koma nsonga siiri kosuntira. Kuti ntundu udzauka pa 8
ntundu, ndi dziko pa dziko: kudzali zibvomezi m' malo ena;
kudzali dzaola: zintu zimenezi ziri zoiamba za tshisoni.

Koma tshenjerani inu noka: kuti adzakuperekani ku 9
magulu a ankoswe; ndi m' masinagoge mudzakwapulidwa;
ndimo patsogolo akuweruza ndi mafumu otshuka mudzaima
kwa ine, kwa kumariza kwa awo. Ndimo patsogolo ivangeli 10
ukanauzidwa kwa mitundu yonse. Ndimo ntawi adzatso- 11
goza inu *kwa kuweruza*, nadzapereka inu, musaganizaganiza
patsogolo tshomwe mudzalankula: koma tshomwe tshidza-
patsidwa kwa inu mwa ora limene, tshomwe mulankula: kuti
simuli inu nomwe mulankula, koma Nzimu Woyera. Ndimo 12
mpwatshi adzapereka mpwatshi kwa imfa, ndi atate mwana
watshi; ndimo ana adzaimirira pa atatu ao ndi amai ao, ndimo
adzapanga awo ku pedwa. Ndimo mudzakwiiridwa ndi antu 13
onse kwa dzina langa: koma emwe akalabe ku nsonga,
amene adzapulumutsidwa.

Koma ntawi muona kunyansa kwa dzinja kuima komwe 14
sikukanaima (emwe awerenga adziwe), pomwe omwe akala
m' Yudeya atawire m' mapiri: ndimo emwe ali pamwamba 15
pa nyumba asatsike, kapena ku loa umo, ku tshotsa kantu
kwa nyumba yatshi: ndi emwe ali m' munda asabwere ku 16
tenga tshopfunda tshatshi. Koma kwaipa ku awa omwe ali 17
ndi mimba ndi ku awa omwe amwitsa m' masiku awo! Ndimo 18
pemperani kuti sikuli m' malimwe. Kuti masiku awo 19
adzali sautso, yotere monga siinali yofana kwa kwiamba
kwa kupanga komwe Mulungu anapanga kwa tsopano,
ndimo siidzali ntawi ina. Ndimo ngati Mwini sanafupitsa 20
masiku, palibe nyama ikanapulumutsidwa: koma kwa osang'-
kidwa, omwe anasang'ka, anafupitsa masiku. Ndimo pomwe 21
ngati muntu modzi adzanena ndi inu, Ona, Kristu ali pano;
kapena, Ona, uko; musamvana: kuti adzauka Akristu 22
onyenga ndi aprofeti onyenga, nadzasonya zizindikilo ndi
zozizwa, kuti angosotshereza, ngati adziwa, osang'kidwa.
Koma yang'anirani: ona, daambirira inu ndi zintu zonse. 23

Koma m' masiku awo, pambuiu sautso imene, dzua lidza- 24

25 detsedwa, ndi mwezi sudzapatsa kuunika kwatshi, ndimo
nyenyezi zidzalikugwa kwa kumwamba, ndi mpamvu zomwe
26 ziri m' miamba zidzatuntumiritswa. Ndimo pomwe adzaona
Mwana wa muntu adza m' mitambo ndi mpamvu yeikuru
27 ndi kupambana. Ndimo pomwe adzatumiza anjelo, ndimo
adzasong'ketsa osang'kidwa atshi kwa mpepo zinai, kwa
pande lakutali la dziko kwa pande lakutali la kumwamba.
28 Ndimo kwa ntengo wa nkhuyu punzirani fanizo latshi:
ntawi ntambi yatshi ikala yotepa, niturutsa masamba atshi,
29 mudziwa kuti dzinja liri pafupi; inde tshointshi inu unso,
ntawi muona zintu zimenezi zirikukala, mudziwa kuti ali
30 pafupi, *inde* pa dzitseko. Dinena ndi inu nditu, Fuko
limene losadzapita, kwa ntawi zintu zonse zimenezi zidza-
31 tedwa. Kumwamba ndi dziko zidzapita: koma mau anga
32 sadzapita. Koma ndi siku limene kapena ora limene palibe
modzi adziwa, si inde anjelo m' mwamba, kapena Mwana,
33 koma Atate. Yang'anirani, dikirani ndi pemperani: kuti
34 musadziwa ntawi iti. *Iri* monga *ntawi* muntu, ali mlendo m'
dziko lina, nasia nyumba yatshi, napatsa mpamvu ku akapolo
atshi, kwa onse ntshito yatshi, nauza anso tsatshipata ku
35 dikira. Ndimo mudikire: kuti musadziwa ntawi mwini wa
nyumba adza, kapena pa madzulo, kapena pakati pa usiku,
36 kapena pa kulira kwa tambala, kapena m' mawa; kani
37 kudza nsanga akupezani mulikugona. Ndi tshomwe dinena
ndi inu dinena ndi onse, Dikirani.

14 Ndimo pambuiu pa masiku awiri kunali *kudia kwa*
mpasika ndi nkate wopanga tshabe: ndimo adzukuru akuru
ndi akulembera nafuna bwanje anangomgwira ndi tshinyengo,
2 nangompa: kuti anati, Si muntawi ya kudia, kani kapena
kudzali pokoso la antu.

3 Ndimo ntawi anali m' Betaniya m' nyumba ya Simon
wakate, monga analikukala pa kudia, nadza nkazi anali
nayo nsupa ya alabastile ya mafuta a nardo ntengo watshi
wapatali; *ndimo* naswa nsupa, natsanula pa mutu patshi.
4 Koma anali ena omwe anali ndi kukwia mwa awo oka, *kuti*,
Kwa kuyerekeza kwanje kusakaza kumene kwa mafuta
5 kwapangidwa? Kuti mafuta amene anangogulitsidwa kwa
madenariyon opambana mazana atatu, anangopatsidwa kwa
6 osauka. Ndimo anang'ung'udza pa ie. Koma Yesu nati,
Lekani ie; mumvuta bwanje? watshita ntshito yabwino pa
7 ine. Kuti mupotshera osauka ndi inu ntawi zonse, ndimo
ntawi yomwe mufuna mudziwa ku tshita zabwino nao:

koma ine musapotshera ntawi zonse. Watshita tshomwe 8
wadziwa: wadzosa tupi langa patsogolo kwa kuika m'
mwanda. Ndimo dinena ndi inu nditu, Pomwe ivangeli 9
udzauzidwa mwa dziko lonse, tshimene enso tshomwe nkazi
amene watshita tshidzalankulidwa kwa tshikumbutso tsha ie.

Ndimo Yuda Sikariyoti, iemwe anali modzi wa kumi ndi 10
awiri, nang'ka kwa adzukuru akuru, kuti apereke ie kwa
awa. Ndimo awa, ntawi anamva, nasekera, nalonjezana ku 11
patsa ie ndrama. Ndimo nafuna bwanje anangompereka
kopepuka *kwa awa.*

Ndimo pa siku loamba la nkate wopanga tshabe, ntawi 12
anatsira mpasika, akupunzira atshi anena nai', Pati ufuna
kuti ting'ke ku fotokoza kuti ungodia mpasika? Ndimo 13
atumiza awiri a akupunzira atshi, nanena nao, Mukani
muzinda, ndimo adzakomana ndi inu muntu anyamula mbia
ya madzi: tsatani ie; ndimo pomwe adzaloa, nenani ku 14
mwini wa nyumba, Mpunzitsi ati, Tshipinda tshanga tsha
olendo tshiri kuti, komwe didzadia mpasika ndi akupunzira
anga? Ndimo adzasonya ie eka tshipinda tshatshikuru tsha- 15
pamwamba ndi zintu ziri umo *ndimo* tshafotokozedwa: ndimo
apo fotokozerani ife. Ndimo akupunzira naturuka, nadza 16
muzinda, napeza monga nanena nao: nafotokoza mpasika.

Ndimo madzulo, adza ndi kumi ndi awiri. Ndimo monga 17, 18
nakala nalinkudia, Yesu nati, Dinena ndi inu nditu, Modzi
wa inu adzandizonda, *inde* emwe adia ndi ine. Anaamba 19
ku kala ndi tshisoni, ndi ku nena nai' modzi ndi modzi,
Kodi ndine? Ndimo nanena nao, *Ali* modzi wa kumi ndi 20
awiri, emwe asunsa ndi ine m' mbale. Kuti Mwana wa 21
muntu apita, inde monga alembedwa ndi ie: koma tshaipa
kwa muntu amene ndi emwe Mwana wa muntu azondedwa!
kunali bwino ku muntu amene ngati sanabadwa.

Ndimo monga analinkudia, natenga nkate, ndimo ntawi 22
anadalitsa, nauswa, napatsa ku awa, nati, Tengani: umeneu
uli tupi langa. Ndimo natenga tshiko, ndimo ntawi anati 23
tshakoma, napatsa ku awa: ndimo onse namwa ndi itsho.
Ndimo nanena nao, Umene uli mwazi wanga wa testamente, 24
womwe uturutsidwa kwa ambiri. Dinena ndi inu nditu, 25
sindidzamwa anso ndi tshobala tsha mvina, kwa siku lomwe
ntawi dimwa ndi itsho tshatsopano m' dziko la Mulungu.

Ndimo ntawi naimba nyimbo, naturuka ku piri la 26
Maolive.

Ndimo Yesu anena nao, Inu nonse mudzakwiitsidwa: 27

tshifuka kuti alembedwa, Didzakoma mbusa, ndi nkosa
28 zidzabalalitsidwa. Koma, pambuiu diukitswa, didzaenda
29 patsogolo pa inu m' Galileya. Koma Petros nanena nai',
30 Ngati onse adzakwiitsidwa, kosuntira si ndine. Ndimo Yesu
anena nai', Dinena ndi iwe nditu, kuti iwe lero, *inde* usiku
uno, patsogolo tambala alira kawiri, undikana katatu.
31 Koma nanena kolimba kopambana, Ngati dikanafa ndi iwe,
sindidzakana iwe. Ndimo tshointshi inso nanena onse.
32 Ndimo nadza ku malo omwe anatshedwa Getsemane:
ndimo anena ndi akupunzira atshi, Kalani pano, ntawi
33 dipempera. Ndimo atenga nai' Petros ndi Yakobi ndi
Yohane, naamba ku zizwa kwambiri, ndi ku kala ndi nsoni
34 zambiri. Ndimo anena nao, Nzimu wanga uli ndi tshisoni
tshambiri inde kwa imfa: kalani pano, ndi dikirani.
35 Ndimo napita patsogolo pang'ono, nagwa pansi, napempera
36 kuti, ngati kunali kuteka, ora linangopita kwa ie. Ndimo
nanena, Aba, Atate, zintu zonse ziri zoteka kwa iwe; sunta
tshiko tshimenetshi kwa ine: koma si tshomwe difuna,
37 koma tshomwe ufuna. Ndimo adza, napeza awa alikugona,
nanena ndi Petros, Simon, kodi ugona? kodi sudziwa ku
38 dikira ora limodzi? Dikirani ndi pemperani, kuti musaloa
m' tshinyengo: nzimu ulikufuna nditu, koma nyama ilefuka.
39 Ndimo onso namuka, napempera, kunena mau amodzimodzi.
40 Ndimo onso nafika, napeza awa alikugona, kuti maso ao
anali olemera kwambiri; ndimo sanadziwa bwanje kuiang'ka
41 ie. Ndimo adza ntawi yatshitatu, nanena nao, Gonani
tsopano, tengani kupuma kwanu: kuli kukwana; ora
linadza; ona, Mwana wa muntu azondedwa m' manja a
42 ampulupulu. Dzukani, tidzing'ka: ona, iemwe azonda ine
ali pafupi.
43 Ndimo tsopano lino, ntawi kosuntira analikunena, Yuda
adza, modzi wa kumi ndi awiri, ndimo ndi ie antu ambiri
ndi mipeni ya nkondo ndi zindodo, kwa adzukuru akuru ndi
44 akulembera ndi akuru. Ndimo emwe anamzonda wapatsa
awa tshizindikilo, kuti, Emwe didzamsomsona, emwe ali ie;
45 mgwireni, mtsogozeni bwino. Ndimo ntawi anadza, tsopano
46 lino nadza kwa ie, ndimo ati, Rabi; namsomsona. Ndimo
47 naika manja pa ie, namgwira. Koma modzi wa awo omwe
anaima pafupi naturutsa mpeni watshi wa nkondo, namenya
48 kapolo wa ndzukuru wang'kuru, nasenga kutu latshi. Ndimo
Yesu naiang'ka nanena nao, Kodi muturuka, monga pa
wolanda, ndi mipeni va nkondo ndi zindodo kundigwira?

Masiku onse dinali ndi inu m' tempile kupunzitsa, ndimo 49
musandigwira: koma *tshimene tshitshitidwa* kuti malemba
anangodzazidwa. Ndimo onse namleka, natawa. 50
Ndimo nyamata modzi anatsata ndi ie, anali ndi nsaru ya 51
lini yopfundila ndi ie, pa *tupi latshi* lamarisetshe: ndimo
amgwira; koma nasia nsaru ya lini, natawa wamarisetshe. 52
Ndimo natsogoza Yesu ku ndzukuru wang'kuru: ndimo 53
asong'kana ndi ie adzukuru akuru onse ndi akuru ndi akule-
mbera. Ndimo Petros anamtsata kutali, inde momo, m' bwalo 54
la ndzukuru wang'kuru; ndimo analikukala ndi akazembe,
naota m' kuunika *kwa moto*. Ndimo adzukuru akuru ndi 55
gulu lonse la ankoswe nafunira kumariza pa Yesu kumpa;
napeza palibe. Kuti ambiri nasinjirira pa ie, ndimo kumariza 56
kwao sikunafana. Ndimo naima ena, nasinjirira pa ie, kuti, 57
Tinamva ie ku ti, Didzamwaza malo oyera amene omwe 58
apangidwa ndi manja, ndimo m' masiku atatu didzamanga
ena opangidwa opanda manja. Ndimo inde si tshointsho 59
kumariza kwao kunafana. Ndimo ndzukuru wang'kuru 60
naima pakati, nafunsa Yesu, kuti, Suiang'ka kantu? tshiri
tshiani tshomwe amene amariza pa iwe? Koma nato- 61
ntola, sanaiang'ka kantu. Anso ndzukuru wang'kuru
namfunsa, ndimo anena nai', Kodi uli Kristu, Mwana wa
Wodala? Ndimo Yesu nati, Diri: ndimo mudzaona Mwana 62
wa muntu kukala pa dzanja lamanja la mpamvu, ndi kudza
ndi mitambo ya kumwamba. Ndimo ndzukuru wang'kuru 63
nang'amba nsaru zatshi, ndimo anena, Tifuna bwanje kopa-
mbana omariza? Mwamva kutukwana: muganiza tshiani? 64
Ndimo awa onse namsutsa ku enera kwa imfa. Ndimo ena 65
naamba ku labvula mate pa ie, ndi ku pimba nkope yatshi,
ndi ku bafamula ie, ndi ku nena nai', Losa: ndi akazembe
namlandira ndi mabafamulo a manja ao.

Ndimo monga Petros anali pansi m' bwalo, lidza kwa ie 66
limodzi la mautu a ndzukuru wang'kuru: ndimo kuona 67
Petros kuota, linayang'ana pa ie, nalinena, Ndiwe enso
unali ndi Mnazarete, *inde* Yesu. Koma nakana, kuti, 68
Sindidziwa, kapena sindidziwitsa tshomwe utshinena:
ndimo naturuka ku balanda; ndimo tambala nalira.
Ndimo butu linamona, ndimo linaamba anso ku nena ndi 69
awo omwe naima pafupi, Amene ali *modzi* wa awa. Koma 70
anso nakana. Ndimo pambuiu ntawi yeing'ono onso awo
omwe naima pafupi nanena ndi Petros, Wa nteradi uli
*modzi* wa awa; kuti uli Mgalileya. Koma naamba ku 71

tukwana, ndi ku lumbira, Sindidziwa muntu amene wa
72 emwe munena. Ndimo tsopano lino ntawi yatshiwiri tambala
nalira. Ndimo Petros nakumbukila mau, bwanje kuti Yesu
nanena nai', Patsogolo tambala alira kawiri, udzakana ine
katatu. Ndimo ntawi naganiza ndi amene, nalira nsozi.

15 Ndimo tsopano lino mamawa adzukuru akuru ndi akuru
ndi akulembera, ndi gulu lonse la ankoswe, naweruzana, na-
2 manga Yesu, namtsogoza, nampereka kwa Pilato. Ndimo
Pilato namfunsa, Kodi uli Fumu Yotshuka ya Ayuda? Ndimo
3 ie kuiang'ka anena nai', Uti. Ndimo adzukuru akuru natshula
4 ie ndi zintu zambiri. Ndimo Pilato namfunsa anso, kuti,
5 Suiang'ka kantu? ona zintu zingati azitshula pa iwe. Koma
Yesu sanaiang'ka kantu unso; monga kuti Pilato nazizwa.
6 Ndimo pa kudia nazolowera ku masula kwa awo womangi-
7 dwa modzi, emwe anafunsa kwa ie. Ndimo kunali modzi
atshedwa Baraba, womangidwa ndi awo omwe anapenduka,
8 antu omwe mwa kupenduka natshita mbanda. Ndimo antu
ambiri nakwera naamba ku funsa ie *ku tshita* monga
9 anazolowera ku tshita nao. Ndimo Pilato naiang'ka awo,
kuti, Kodi mufuna kuti dimasule kwa inu Fumu Yotshuka
10 ya Ayuda? Kuti nadziwitsa kuti kwa dano adzukuru akuru
11 anapereka ie. Koma adzukuru akuru nakantshizira antu
12 ambiri, kuti kopambana akamasula nao Baraba. Ndimo
Pilato naiang'ka anso nanena nao, Ndimo didzatshita tshiani
13 kwa emwe mutsha Fumu Yotshuka ya Ayuda? Ndimo
14 napfula anso, Patshika ie. Ndimo Pilato nanena nao,
Bwanje, tshaipa ndi tshiani watshita? Koma napfula kwa-
15 mbiri, Patshika ie. Ndimo Pilato, kufuna ku sekeretsa
antu ambiri, namasula kwa awo Baraba, napereka Yesu,
ntawi anamkwapula, ku patshikidwa.
16 Ndimo ankhondo namtsogoza m' bwalo, lomwe liri Pre-
17 torium; ndimo asong'kanitsa gulu lonse. Ndimo abveka ie
ndi nsaru yakuda, ndi kuluka tshisoti tshotshuka tsha
18 minga, natshiika pa ie; ndimo naamba ku utsa ie, A, Fumu
19 Yotshuka ya Ayuda! Nagogoda mutu watshi ndi nzengo,
nalabvula mate pa ie, ndi kugwada maondo ao napembedza
20 ie. Ndimo ntawi natonza ie, nabvula nsaru yakuda kwa ie,
naika miinjiro yatshi pa ie. Ndimo atsogoza ie ku patshika ie.
21 Ndimo akakamiza modzi alikupita, Simon kwa Kirene,
kudzera minda, atatu atshi a Alesandire ndi Rufo, ku enda
22 *nao*, kuti anangonyamula nkhwitshi yatshi. Ndimo amtenga
ku malo Golgota, lomwe liri, kusandukidwa, Malo a pala.

Ndimo napatsa ie vinyo wosang'kanizidwa ndi more: koma 23
sanalandira. Ndimo ampatshika, nagawana miinjiro yatshi 24
mwa awo, kuyesa ndi iyo, yomwe onse akatenga. Ndimo 25
linali ora latshitatu, napatshika ie. Ndi lemba la kutshula 26
kwatshi linalembedwa pamwamba, FUMU YOTSHUKA YA
AYUDA. Ndimo ndi ie apatshika olanda awiri; modzi pa 27
dzanja lamanja latshi, ndi wina pa dzanja lamanzere latshi.
Ndimo awo omwe anapita natukwana ie, kupukusa mitu yao, 29
ndi kuti, Ha! iwe emwe umwaza malo oyera, nuamanga
m' masiku atatu, udzipulumutse, nutsika pa nkhwitshi. 30
Tshointshi inso adzukuru akuru kutonza *ie* mwa awo oka 31
ndi akulembera nati, Napulumutsa ena, wosadziwa ku dzi-
pulumutsa. Kristu, Fumu Yotshuka ya Sirayeli, atsike 32
tsopano pa nkhwitshi, kuti tione ndimo timvane. Ndi omwe
anapatshikidwa nai' natonza ie.

Ndimo ntawi ora latshisanu ndi tshimodzi linafika, ulipo 33
ndima m' dziko lonse, kwa ora latshisanu ndi tshinai.
Ndimo pa ora latshisanu ndi tshinai Yesu napfula ndi liu 34
lalikuru, Eloyi, Eloyi, lama sabakatani? omwe ali, kusa-
ndukidwa, Mulungu wanga, Mulungu wanga, unandisira
bwanje? Ndimo ena a awo omwe naima pafupi, ntawi 35
anamva, nati, Ona, aitana Eliya. Ndimo modzi natamanga, 36
nadzaza sponje ndi vinegre, naliika pa nzengo, napatsa ie
ku mwa, kuti, Lekani; tione ngati Eliya adza kum-
tsitsa. Ndimo Yesu napfula ndi liu lalikuru, natsirizika. 37
Ndimo tshopimba tsha malo oyera tshinaganikana kawiri ku 38
mwamba ku pansi. Ndimo ntawi kenturione, emwe naima 39
pafupi pandunji pa ie, naona kuti tshointsho natsirizika,
nati, Muntu amene anali Mwana wa Mulungu nditu.
Ndimo kunali inso akazi kuyang'anira kutali: mwa iwo 40
*anali* Mariya kwa Magadala, ndi Mariya amai atshi a
Yakobi wang'ono ndi Yose, ndi Salome; omwe, ntawi anali 41
m' Galileya, namtsata, naimirira kwa ie; ndi akazi ambiri
ena omwe nakwera ndi ie kwa Yerusalem.

Ndimo ntawi tsopano madzulo nadza, tshifuka kunali Kuko- 42
nzetsa, komwe kuli, dzua lapatsogolo sabata, kunadza Yosefe 43
kwa Arimateya, nkoswe waulemu, emwe enso ie eka analiku-
yang'anira dziko la Mulungu; ndimo naloa kolimbika kwa
Pilato, napempa ntembo wa Yesu. Ndimo Pilato nazizwa ngati 44
patsogolo anafa: ndimo kuitana kwa ie kenturione, nafunsa
ie ngati wafa kali. Ndimo ntawi nadziwa ndi kenturione, 45
napatsa ntembo kwa Yosefe. Ndimo nagula nsaru ya lini, 46

ndimo kumtsitsa nammanga ndi nsaru ya lini, namika m'
mwanda womwe unafulidwa m' tantwe; nagubuduza mwala
47 ku komo la mwanda. Ndimo Mariya kwa Magadala ndi
Mariya *amai atshi* a Yose naona pomwe anaikidwa.
16 Ndimo ntawi sabata linapita, Mariya kwa Magadala, ndi
Mariya *amai atshi* a Yakobi, ndi Salome, anagula zonung'-
2 kira zabwino, kuti anangofika nadzosa ie. Ndimo mamawa
siku lakuamba la wiki, adza ku mwanda ntawi dzua lina-
3 turuka. Ndimo analikuuzana, Adzagubuduzira mwala pa
4 komo la mwanda ndani? ndimo kuyang'ana, aona kuti
5 mwala ugubuduzidwa: kuti unali woukuru nditu. Ndimo
kuloa m' mwanda, naona nyamata kukala pa kundu lamanja,
6 wabvala ndi mwinjiro woyera; ndimo nazizwa. Ndimo
anena nao, Musazizwa: mufuna Yesu, Mnazarete, emwe
wapatshikidwa: wauka; siali pano: ona, malo pomwe
7 anamwika! Koma mukani, uzani akupunzira atshi ndi
Petros, Atsogolera inu ku Galileya: uko mudzamona,
8 monga ananena ndi inu. Ndimo naturuka, natawa ku
mwanda; kuti kuntentemera ndi kuzizwa zinafika pa awo:
ndimo sananena kantu ndi modzi; kuti naopa.

9 Ndimo ntawi anauka mamawa pa dzua latshimodzi la wiki,
nadzisonyeza pakwiamba ku Mariya kwa Magadala, mwa
10 emwe anaturutsa ademon asanu ndi awiri. Namuka nauza
awo omwe anali nai', monga anali ndi tshisoni nalira misozi.
11 Ndimo awa, ntawi anamva kuti anali ndi moyo, ndimo
anaonedwa ndi ie, sanamvana.
12 Ndimo pambuiu zintu zimenezi nasonyezedwa m' maka-
lidwe ena kwa awiri a awo, monga naendaenda, pa njira yao
13 m' minda. Ndimo namuka nauza ku omwe atsala: kapena
sanamvana ndi awo.
14 Ndimo pambuiu nadzisonyeza kwa kumi ndi modzi iwo
oka monga nakala pa kudia; ndimo nadzuma awo ndi
kusamvana kwao ndi kulimbika kwa mitima, tshifuka sana-
15 mvana ndi awo omwe anamona pambuiu anauka. Ndimo
nanena nao, Endani ku maiko onse, uzani ivangeli ku opangi-
16 dwa onse. Iemwe amvana ndi ku bapatizidwa adzapulumu-
17 tsidwa; koma iemwe wosamvana adzasutsidwa. Ndimo
zizindikilo zimenezi zidzatsata awo omwe amvana: m' dzina

langa adzaturutsa ademon; adzanena ndi mau atsopano; adza- 18
tukula zinjoka, ndimo ngati amwa kantu kakupa, kosadza-
pweteka awo, adzaika manja pa odwala, ndimo adzatshira.
Tshointsho pomwe Mwini Yesu, pambuiu analankula nao, 19
analandiridwa m' mwamba, nakala pa dzanja lamanja la
Mulungu. Ndimo naturuka, nauza pa malo onse, Mwini 20
kutshita ndi awo, ndi kulimbikitsa mau ndi zizindikilo
zomwe zinatsata. Amen.

# IVANGELI WA LUKA.

TSHIFUKA kuti monga ambiri anayesa ku linganiza 1
ku uza kwa zintu zimenezo zomwe zinadzazidwa mwa
ife, inde monga anazipereka kwa ife, tomwe kwa kuiamba 2
tinali omariza ndi maso ndi oimirira a mau, kunaenedwa 3
bwino kwa ine enso, dinaronda kolimbitsa kupitirira kwa zintu
zonse kwa kuiamba, ku lemba kwa iwe mwa kulinganiza,
Teyofilo wabwino wopambana; kuti unangodziwa ku 4
limbitsa kwa mau m' omwe unapunzitsidwa.

Kunali m' masiku a Herode, fumu yotshuka ya Yudeya, 5
ndzukuru modzi atshedwa Zekariya, wa gulu la Abiya:
ndimo anali ndi nkazi wa ana akazi a Haron, ndi dzina
latshi linali Elizabete. Ndimo awa awiri anali odeka 6
patsogolo Mulungu, kuendaenda m' mau onse ndi m'
miambi ya Mwini opanda tshimo. Ndimo anali opanda 7
mwana, tshifuka kuti Elizabete anali tshimbwira, ndimo
awa awiri anali ndi dzaka dzambiri.

Ndimo kunali, ntawi natshita ntshito ya ndzukuru 8
patsogolo Mulungu m' kurondetsa kwa gulu latshi, kwa 9
ntengo wa ntshito ya ndzukuru, kuyesa kwatshi kunali ku
loa m' malo oyera a Mwini ndi ku fukiza zonung'kira.
Ndimo antu onse ambiri analikupempera kunja pa ora la 10
zonung'kira. Ndimo nasonya kwa ie njelo wa Mwini kuima 11
pa kundu lamanja la katshisi wa zonung'kira. Ndimo 12
Zekariya nantuntumiridwa ntawi namona, ndimo kuopa

13 kunadza pa ie. Koma njelo nanena nai', Usaopa, Zekariya:
tshifuka pempo lako linamveka, ndi nkazi wako Elizabete
adzabala mwana wamamuna ndi iwe, ndimo udzatsha dzina
14 latshi Yohane. Ndimo udzakala ndi tshimwemwe ndi kuko-
ndwera; ndimo ambiri adzasekera pa kubadwa kwatshi.
15 Kuti adzakala wang'kuru m' kuona kwa Mwini, ndimo
sadzamwa kapena vinyo kapena kumwa kwakulimba;
ndimo adzadzazidwa ndi Nzimu Woyera, inde kwa tshibaliro
16 tsha amai atshi. Ndimo ambiri a ana a Sirayeli adzatembe-
17 nuza ku Mwini, Mulungu wao. Ndimo adzaenda patsogolo
pa nkope yatshi m' nzimu ndi m' mpamvu za Eliya, ku
tembenuza mitima ya atatu ao ku ana, ndi osamvera *ku enda*
m' nzeru za odeka; ku panga kuta kwa Mwini antu
18 okonzetsedwa *kwa ie.* Ndimo Zekariya nanena ndi njelo,
Bwanje didzadziwa tshimene? kuti diri muntu wankalamba,
19 ndi nkazi wanga anali ndi dzaka dzambiri. Ndimo njelo
kuiang'ka nanena nai', Diri Gabriyeli, emwe diima patsogolo
pa nkope ya Mulungu; ndimo dinatumidwa ku lankula
20 ndi iwe, ndi ku uza iwe mau amene abwino. Ndimo ona,
udzakala watshete nusadziwa ku lankula, kwa siku lomwe
zintu zimenezi zidzatshitidwa, tshifuka usanamvana mau
21 anga, omwe adzadzazidwa pa ntawi yao. Ndimo antu
analikulindira Zekariya, nazizwa ndi kutshedwa kwatshi m'
22 malo oyera. Ndimo ntawi naturuka, sanadziwa ku lankula
nao: ndimo nadziwitsa kuti anaona kuona m' malo oyera:
ndimo analikukodola kwa awo, nakalabe wosadziwa ku
23 lankula. Ndimo kunali, ntawi masiku a kuimirira kwatshi
anata, nang'ka ku nyumba yatshi.
24 Ndimo pambuiu masiku amene Elizabete nkazi watshi
25 nabvuuka; nabisala ie eka miezi isanu, kuti, Tshointshi
Mwini watshita ndi ine m' masiku m' omwe wayang'anira pa
*ine*, ku tshotsa kusinjirira kwanga mwa antu.
26 Ndimo m' mwezi watshisanu ndi tshimodzi njelo Gabriyeli
anatumidwa ndi Mulungu ku mzinda wa Galileya, utshedwa
27 Nazarete, ku tshiweta wapalidwa ndi muntu dzina latshi
linali Yosefe, wa nyumba ya Davide; ndi dzina la tshiweta
28 linali Mariya. Ndimo naloa kwa ie, nati, Ea, woanjanidwa,
29 Mwini *ali* ndi iwe. Koma nantuntumiridwa kwambiri ndi
30 mau, naganiza kuutsa kwanje kumene kungokala. Ndimo
njelo nanena nai', Usaopa, Mariya: kuti wapeza kuanjana
31 ndi Mulungu. Ndimo ona, udzabvuuka m' tshibaliro
tshako, nudzabala mwana wamamuna, nudzatsha dzina

latshi Yesu. Adzakala wang'kuru, nadzatshedwa Mwana 32
wa Wopambanitsa: ndi Mwini Mulungu adzapatsa kwa ie
mpando wotshuka wa atatu atshi Davide: ndimo adza- 33
weruza pa nyumba ya Yakobi kwa magonero; ndimo ndi
dziko latshi kudzakala palibe kumariza. Ndimo Mariya 34
nanena ndi njelo, Bwanje tshimene tshidzakala, monga
sindidziwa muntu? Ndimo njelo naiang'ka nanena nai', 35
Nzimu Woyera udzafika pa iwe, ndi mpamvu ya
Wopambanitsa idzapimba iwe: ndimo onso itsho tshomwe
tshidzabadwa tshidzatshedwa tshoyera, Mwana wa Mulungu.
Ndimo ona, Elizabete mbali wako, ie enso wabvuuka 36
mwana wamamuna mwa utali wa kugonera kwatshi: ndi
umene uli mwezi watshisanu ndi tshimodzi ndi ie emwe
natshedwa tshimbwira. Kuti palibe mau kwa Mulungu 37
adzakala opanda mpamvu. Ndimo Mariya nati, Ona, 38
ndzakazi wa Mwini; tshikale ndi ine tshofana ndi mau ako.
Ndimo njelo natshoka kwa ie.

Ndimo Mariya nauka m' masiku adya naenda m' dziko 39
lamapiri ndi tshangu, m' mzinda wa Yuda; naloa m' 40
nyumba ya Zekariya nautsa Elizabete. Ndimo kunali, 41
ntawi Elizabete anamva kuutsa kwa Mariya, kanda linalumpa
m' tshibaliro tshatshi; ndi Elizabete nadzazidwa ndi Nzimu
Woyera; ndimo nalankula ndi kupfula kwakukuru, nati, 42
Wodala *uli* iwe mwa akazi, ndi wodala *ali* wobala wa
tshibaliro tshako. Ndimo bwanje tshiri tshimenetshi kwa 43
ine, kuti amai a Mwini wanga akadza kwa ine? Kuti ona, 44
ntawi liu la kuutsa kwako linafika m' makutu anga, kanda
linalumpa m' tshibaliro tshanga kwa tshimwemwe. Ndimo 45
wodala *ali* ie emwe namvana; kuti kudzakala kumariza kwa
zintu zomwe zalankulidwa ndi ie kwa Mwini. Ndimo 46
Mariya wati,

Moyo wanga ukulitsa Mwini,
Ndi nzimu wanga wasekera ndi Mulungu Mpulumutsi 47
wanga.
Kuti wayang'anira kusauka kwa ndzakazi watshi: 48
Kuti ona, kwa ntawi yatsopano mafuko onse adzatsha
ine wodala.
Kuti emwe ali wampamvu watshita kwa ine zintu 49
zazikuru;
Ndi loyera liri dzina latshi.
Ndi nsisi yatshi iri kwa mafuko ndi mafuko 50
Pa awo omwe aopa ie.

51 Wasonyeza mpamvu ndi nkono watshi;
Wabalalitsa akudzitama mwa kuganiza kwa mitima yao.
52 Watsitsa ampamvu kwa mipando yotshuka *yao*,
Ndi wapambanitsa awa osauka.
53 Anjala wakutitswa ndi zintu zabwino;
Ndi olemera watumiza tshabe.
54 Watangata Sirayeli mwana watshi,
Kuti anangokumbukila nsisi
55 (Monga nalankula ndi atatu atu)
Kwa Abraham ndi kwa mbeu yatshi, kwa ntawi yonse.
56 Ndimo Mariya nakala ndi ie kwa miezi itatu, nabwera ku
nyumba yatshi.
57 Ndimo ntawi ya Elizabete inakwana ku bala; ndimo
58 wabala mwana wamamuna. Ndimo oiandikila atshi ndi
abali atshi namva kuti Mwini anakulitsa nsisi yatshi kwa ie;
59 ndimo anasekera nai'. Ndimo kunali, pa siku latshisanu
ndi tshitatu, kuti nadza ku dula mwana; ndimo anali
kumtsha Zekariya, pambuiu pa dzina la atatu atshi.
60 Ndimo amai atshi naiang'ka nati, Si tshointshi; koma
61 adzatshedwa Yohane. Ndimo nanena nai', Kulibe modzi
62 wa abali ako emwe atshedwa ndi dzina limene. Nakodola
63 ku atatu atshi, lanje akafuna kumtsha. Ndimo nafunsira
kagome kolembera, nalemba, kuti, Dzina latshi liri Yohane.
64 Ndimo onse nazizwa. Ndimo nkamwa mwatshi munatse-
gulidwa tsopano lino, ndi lilume latshi *linamasulidwa*,
65 nalankula, kudalitsa Mulungu. Ndimo kuopa kunafika pa
onse omwe nakala kozungulira awa: ndi mau onse amenewa
66 nauzidwa mwa dziko lonse lamapiri la Yudeya. Ndimo
onse omwe anamva naika awo m' mitima yao, kuti, Nanga
bwanje mwana amene adzakala? Kuti dzanja la Mwini
linali nai'.
67 Ndimo atatu atshi Zekariya anadzazidwa ndi Nzimu
Woyera, nalosa, kuti,
68 Wodala *akale* Mwini, Mulungu wa Sirayeli;
Kuti watsheza ndimo watshita kuombola kwa antu atshi,
69 Ndimo watukulitsa nyanga ya kupulumutsa kwa ife
M' nyumba ya mwana watshi Davide
70 (Monga nalankula ndi nkamwa mwa aprofeti atshi oyera
omwe anakala kwa ntawi dziko linaamba),
71 Kupulumutsa kwa mariwongo atu, ndi kwa dzanja la
onse omwe akwiira ife;
72 Ku sonya nsisi kwa atatu atu,

Ndi ku kumbukila kupangana kwatshi kwakuyera;
Lumbiro lomwe nalumbira kwa Abraham atatu atu, 73
Ku patsa kwa ife kuti ife kupulumutsidwa kwa dzanja 74
la mariwongo atu,
Tikaimirira ie opanda kuopa,
M' kuyera ndi m' kudeka patsogolo pa ie masiku onse atu. 75
Inde ndi iwe, mwana, udzatshedwa mprofeti wa Wopa- 76
mbanitsa:
Kuti udzang'ka patsogolo pa nkope ya Mwini ku fotokoza
njira zatshi;
Ku patsa kudziwa kwa kupulumutsa kwa antu atshi 77
M' kubwera kwa zakwaipa zao,
Tshifuka tsha nsisi yabwino ya Mulungu watu, 78
Ndi imene mbanda kutsha mwa kumwamba mudza-
titshezera,
Ku wala pa awo omwe akala mudima ndi m' tshitunzi- 79
tunzi tsha imfa;
Ku tsogoza mapazi atu m' njira ya ntendere.

Ndimo mwana nakula, nalimbika m' nzimu, nali m' 80
zipululu kwa siku la kusonyeza kwatshi kwa Sirayeli.

Ndimo kunali m' masiku adya, naturuka mau kwa Kesare 2
Augusto, kuti dziko lonse likalembedwa. Kumene kunali 2
kulembedwa kwakumwamba kunapangidwa ntawi Kireniyo
anali mbiri wa Siriya. Ndimo onse nang'ka ku dzilemba, 3
onse kwa mzinda watshi. Ndimo Yosefe enso nakwera ku 4
Galileya, ku mzinda wa Nazarete, mwa Yudeya, ku mzinda
wa Davide, womwe watshedwa Betelehem, tshifuka kuti
anali wa nyumba ndi fuko za Davide; ku dzilemba ndi 5
Mariya, emwe anapalidwa ndi ie, ali ndi mimba yeikuru.
Ndimo kunali, ntawi anali apo, masiku anakwana monga 6
kuti akabala. Ndimo nabala mwana wamamuna watshi 7
woiamba; namkuta ndi nsaru, namwika mudiero wa nyama,
tshifuka kuti palibe malo kwa awo m' bwalo.

Ndimo kunali m' dziko limene abusa kukala m' munda, 8
ndi kuyang'anira gulu lao usiku. Ndimo njelo wa Mwini 9
naima ndi awo, ndi kupambana kwa Mwini kunawala
kozungulira awo: ndimo naopa kwambiri. Ndimo njelo 10
nanena nao, Musaopa; kuti ona, ditengera inu mau abwino
a tshimwemwe tshatshikuru omwe adzali ku antu onse: kuti 11
kwa inu wabadwa lero m' mzinda wa Davide Mpulumutsi,
iemwe ali Kristu Mwini. Ndimo tshimene *tshiri* tshizi- 12
ndikilo kwa inu; Mudzapeza kanda wakutidwa ndi nsaru, ndi

13 kugona mudiero. Ndimo kwansangu kunali ndi njelo
ambiri a gulu lamwamba kulemekeza Mulungu, ndi kunena,
14 Kupambana kwa Mulungu mo pambanitsa,
Ndi pansi ntendere mwa antu, mwa omwe asekera bwino.
15 Ndimo kunali, ntawi anjelo anamuka kwa awo m'
mwamba, abusa nanena modzi kwa wina, Tieni tsopano inde
kwa Betelehem, tione tshintu tshimenetshi tshomwe tshinali,
16 tshomwe Mwini anadziwitsa kwa ife. Ndimo naenda ndi
tshangu, napeza Mariya ndi Yosefe, ndi kanda kugona
17 mudiero. Ndimo ntawi naliona, nadziwitsa ndi mau omwe
18 ananenedwa kwa awo ndi kanda limene. Ndimo onse
omwe anamva nazizwa ndi zintu zomwe zinalankulidwa
19 kwa awo ndi abusa. Koma Mariya nasunga mau onse
20 amenewa, naaganizaganiza mutima mwatshi. Ndimo abusa
nabwera, kupambanitsa ndi kulemekeza Mulungu kwa
zintu zonse zomwe anazimva naziona, inde monga kunala-
nkulidwa ku awo.
21 Ndimo ntawi masiku asanu ndi atatu anakwana kwa
kudula ie, dzina latshi linatshedwa Yesu, lomwe linatshedwa
tshointsho ndi njelo patsogolo naamba ku bvuukidwa m'
tshibaliro.
22 Ndimo ntawi masiku a kusamba kwao ofana ndi mau a
Moses anakwana, namtenga kwa Yerusalem, kumpereka
23 kwa Mwini (monga kulembedwa m' mau a Mwini, Amuna
onse omwe atsegula tshibaliro adzatshedwa oyera kwa
24 Mwini), ndi ku tsira nsembe kofana amene omwe anenedwa
m' mau a Mwini, Njiwa ziwiri, kapena maunda awiri
25 ang'ono. Ndimo ona, kunali muntu m' Yerusalem, dzina
la emwe linali Simon; ndi muntu amene anali wodeka ndi
wopembedza, kulindira kwa kusangalatsa kwa Sirayeli: ndi
26 Nzimu Woyera unali pa ie. Ndimo tshinasonyezedwa kwa ie
ndi Nzimu Woyera, kuti sakaona imfa, patsogolo anaona
27 Kristu wa Mwini. Ndimo nafika ndi Nzimu mwa tempile:
ndimo ntawi atatu atshi ndi amai atshi naloeza kamwana
Yesu, kuti anangotshitira ie kofana ndi mwambi wa mau,
28 ndimo namlandira pa mikono yatshi, nadalitsa Mulungu, nati,
29 Tsopano uleke kapolo wako ku muka, O Mbuiye,
Ofana ndi mau ako, m' ntendere;
30 Kuti maso anga anaona kupulumutsa kwako,
31 Komwe wakonzetsa patsogolo pa nkope ya antu onse;
32 Kuunika kwa kusonyeza kwa Mitundu,
Ndi kupambana kwa antu ako Sirayeli.

Ndimo atatu atshi ndi amai atshi analikuzizwa ndi zintu 33
zomwe zinalankulidwa ndi ie; ndimo Simon nadalitsa awa, 34
nanena ndi Mariya amai atshi, Ona *mwana* amene aikidwa
kwa kugwa ndi kuuka kwa ambiri mwa Sirayeli: ndi kwa
tshizindikilo tshomwe tshilankulidwa pa *itsho;* inde ndi 35
mpeni wa nkondo udzabola nzimu wako; kuti maganizo a
mitima yambiri angosonyezedwa. Ndimo kunali modzi 36
Hana, mprofeti wankazi, mwana wankazi wa Fanuweli, wa
fuko la Asheri (anali ndi kugonera kwambiri, nakala ndi
mamuna dzaka dzisanu ndi dziwiri kwa utshiweta watshi,
ndimo anali wamasie inde kwa dzaka makumi asanu ndi 37
atatu, ndi dzinai), iemwe sanatshoka m' tempile, ku
pembedza ndi ku kala wopanda kudia ndi mapempo usiku
ndi usana. Ndimo kufika pa ora limeneli nati tshakoma 38
kwa Mulungu, nalankula ndi ie kwa onse awo omwe
analikuyang'anira kuombola kwa Yerusalem. Ndimo ntawi 39
anakwanitsa zintu zonse zomwe zinali zofana ndi mau a
Mwini, nabwera m' Galileya, ku mzinda wao Naza-
rete.

Ndimo kamwana kanakula, kanalimbika, kanadzaza ndi 40
nzeru: ndi kufatsa kwa Mulungu kunali pa ie.

Ndimo atatu atshi ndi amai atshi nang'ka dzaka dzonse 41
kwa Yerusalem pa kudia kwa mpasika. Ndimo ntawi 42
anali ndi dzaka kumi ndi dziwiri, nakwera kofana ndi
mwambi wa kudia; ndimo ntawi anakwanira masiku 43
monga analikubwera, mwana Yesu nakala pambuiu m'
Yerusalem; ndi atatu atshi ndi amai atshi sanadziwa;
koma kuganiza ie anali m' kamu, naenda ulendo wa siku 44
limodzi; nafunsira ie mwa abali ao ndi anzao: ndimo 45
ntawi sanampeza, nabwera ku Yerusalem, kufuna ie.
Ndimo kunali, pambuiu masiku atatu nampeza m' tempile, 46
kukala pakati pa apunzitsi, kumva awa, ndi kufunsa awa
mafunso: ndimo onse omwe anamva ie nazizwitswa ndi 47
kudziwa kwatshi, ndi kuiang'ka kwatshi. Ndimo ntawi 48
anamona, nazizwa: ndimo amai atshi nanena nai', Mwana,
watshita tshointshi ndi ife bwanje? ona, atatu ako ndi ine
tafuna iwe ndi nsoni. Ndimo nanena nao, Bwanje kuli 49
kuti munafuna ine? musaganiza kuti dikanakala m' nyumba
ya Atatu anga? Ndimo sanadziwa mau omwe nanena nao. 50
Ndimo natsika nao, nafika kwa Nazarete; namvera awa: 51
ndimo amai atshi nasunga mau onse *amenewa* mutima
mwatshi.

52 Ndimo Yesu nakula ndi nzeru ndi msing'ku, ndi m' kufatsa
ndi Mulungu ndi antu.

3 Ndimo m' tshaka kumi ndi tshisanu tsha kuweruza kwa
Tiberiyo Kesare, Pontiyo Pilato anali mbiri wa Yudeya, ndi
Herode anali woweruza wa tshinai wa Galileya, ndi mpwa-
tshi Filipu woweruza wa tshinai wa dziko la Yitureya ndi
la Trakonite, ndi Lisaniyo woweruza wa tshinai wa Abilene,
2 m' udzukuru wa Hana ndi Kayafa, mau a Mulungu
anadza kwa Yohane mwana wa Zekariya m' tshipululu.
3 Ndimo nadza mwa dziko lonse lozungulira Yordan, kuuza
mbapatisma la kutembenuza ntima kwa kubweza kwa
4 zakwaipa; monga alembedwa m' buku la mau a Yesaya
mprofeti,

Liu la modzi kupfula m' tshipululu,
Fotokozani njira ya Mwini,
Lungamitsani njira zatshi.
5 Mipata yonse idzadzazidwa,
Ndi mapiri ndi zitunda zonse zidzateretsedwa;
Ndi kukotakota kudzalungamitsidwa,
Ndi njira zokakalala zidzasalalidwa;
6 Ndi nyama zonse zidzaona kupulumutsa kwa Mulungu.

7 Ndimo nanena ndi antu ambiri omwe naturuka ku
bapatizidwa ndi ie, Inu fuko la zinjoka, watshenjeza inu
8 ndani ku tawa kukwiira kulinkudza? Ndimo balani
dzobala dzoenera dza kutembenuza ntima, ndimo musaamba
ku nena mwa inu noka, Tiri ndi Abraham ali atatu atu:
kuti dinena ndi inu, kuti Mulungu adziwa ndi miala imene
9 ku ukitsa ana kwa Abraham. Ndimo inde tsopano
nkwangwa anso iikidwa pa ntsitsi wa mitengo: ndimo
mitengo yonse yomwe yosabala dzobala dzabwino idulidwa,
10 niponyedwa pa moto. Ndimo antu ambiri nafunsa ie, kuti,
11 Ndimo ife tikanatshita tshiani? Naiang'ka nanena nao,
Iemwe anali ndi maraia awiri, apatse ku emwe alibe; ndi
12 iemwe anali ndi kudia, atshite modzimodzi. Ndimo nadza
anso olandira tsong'ko ku bapatizidwa, nanena nai', Mpunzitsi,
13 tikanatshita tshiani? Ndimo nanena nao, Berani palibe kopa-
14 mbana tshomwe tshinenedwa ndi inu. Ndimo ankhondo onso
nafunsa ie, kuti, Ndimo ife, tikanatshita tshiani? Ndimo
nanena nao, Musatshita nkarwe ndi muntu modzi, kapena
musasinjirira; ndimo mudzakala osekera ndi malipiro anu.

15 Ndimo monga antu analikuyang'anira, ndi antu onse
naganizaganiza m' mitima yao ndi Yohane, ngati kapena

anali Kristu; Yohane naiang'ka, kunena nao onse, Dibapa- 16
tiza inu nditu ndi madzi; koma adza ie emwe ali wolimba
wopambana ine, zingwe za zikwakwata zatshi sindiri woenera
ku masula: adzabapatiza inu ndi Nzimu Woyera ndi moto:
litshero la emwe liri m' dzanja latshi, ku petetsa bwino 17
mbua yatshi, ndimo ku song'ketsa trigu m' nkokwe yatshi;
koma muungu adzaotsha ndi moto wosazima.

Ndimo ndi mayeruzo ambiri ena nauza makalidwe 18
abwino kwa antu; koma Herode woweruza wa tshinai, 19
kusulumulidwa ndi ie kwa Herodiya nkazi wa mbali watshi,
ndi kwa zoipa zonse zomwe Herode anatshita, anaong'khetsa 20
tshimene kopambana zonse, kuti natsekera Yohane m'
nyumba ya ndima.

Ndimo kunali, ntawi antu onse anabapatizidwa, kuti, 21
Yesu unso kunabapatizidwa, ndi kupempera, mwamba
munatsegulidwa, ndimo Nzimu Woyera unatsika mwa 22
makalidwe a tupi, monga njiwa, pa ie, ndi liu linadzera
kumwamba, Uli Mwana wanga wondikonda; mwa iwe
disekera bwino.

Ndimo Yesu eka, ntawi naamba *ku punzitsa*, anali ndi 23
dzaka makumi atatu, ali mwana (monga anaganizidwa) wa
Yosefe, *mwana* wa Heli, *mwana* wa Matati, *mwana* wa Levi, 24
*mwana* wa Maleki, *mwana* wa Yanai, *mwana* wa Yosefe,
*mwana* wa Matatiyo, *mwana* wa Amotse, *mwana* wa Nahum, 25
*mwana* wa Heseli, *mwana* wa Nagai, *mwana* wa Mahati, 26
*mwana* wa Matatiyo, *mwana* wa Shimehi, *mwana* wa Yoseke,
*mwana* wa Yoda, *mwana* wa Yohanan, *mwana* wa Rese, 27
*mwana* wa Zerubabeli, *mwana* wa Shelatiyeli, *mwana* wa
Neri, *mwana* wa Maleki, *mwana* wa Adi, *mwana* wa Kosam, 28
*mwana* wa Alemadam, *mwana* wa Heri, *mwana* wa Yesu, 29
*mwana* wa Eliyezere, *mwana* wa Yoram, *mwana* wa Matati,
*mwana* wa Levi, *mwana* wa Simon, *mwana* wa Yuda, *mwana* 30
wa Yosefe, *mwana* wa Yonam, *mwana* wa Eliyakim, *mwana* 31
wa Maleya, *mwana* wa Mayina, *mwana* wa Mateta, *mwana*
wa Natan, *mwana* wa Davide, *mwana* wa Yese, *mwana* wa 32
Yobede, *mwana* wa Bowaze, *mwana* wa Salimon, *mwana* wa
Nashon, *mwana* wa Haminadabi, *mwana* wa Arni, *mwana* wa 33
Hetseron, *mwana* wa Peretse, *mwana* wa Yuda, *mwana* wa 34
Yakobi, *mwana* wa Yisake, *mwana* wa Abraham, *mwana* wa
Tera, *mwana* wa Nahore, *mwana* wa Seruge, *mwana* wa Rehu, 35
*mwana* wa Pelege, *mwana* wa Hebere, *mwana* wa Shela,
*mwana* wa Kenan, *mwana* wa Arpakshade, *mwana* wa Sheme, 36

37 *mwana* wa Nowa, *mwana* wa Lameki, *mwana* wa Metushela,
*mwana* wa Henoki, *mwana* wa Yeredi, *mwana* wa Mahalalele,
38 *mwana* wa Kenan, *mwana* wa Enoshe, *mwana* wa Sheti,
*mwana* wa Adam, *mwana* wa Mulungu.

4 Ndimo Yesu, wodzaza ndi Nzimu Woyera, nabwera ku
Yordan, natsogozwa ndi Nzimu m' tshipululu kwa masiku
2 makumi anai, ku nyengedwa ndi diabolos. Ndimo m'
masiku amenewo sanadia kantu: ndimo ntawi anakwanidwa,
3 anamva njala. Ndimo diabolos nanena nai', Ngati uli
Mwana wa Mulungu, uza mwala umene kuti upangike nkate.
4 Ndimo Yesu naiang'ka ie, Alembedwa, Muntu wosadzakala
5 ndi moyo ndi mikate yoka. Ndimo namtsogoza, nasonyeza
6 kwa ie maiko onse a dziko m' kantawi kakang'ono. Ndimo
diabolos nanena nai', Kwa iwe, didzapatsa mpamvu yonse
imene, ndi kupambana kwa awo: kuti kwaperekedwa kwa
7 ine; ndi kwa emwe difuna dipatsa iko. Ndimo ngati
udzapembedza patsogolo pa ine, konse kudzakala kwako.
8 Ndimo Yesu naiang'ka nanena nai', Alembedwa, Udzape-
mbedza Mwini Mulungu wako, ndi ie eka udzaimirira.
9 Ndimo namtsogoza kwa Yerusalem, namwika pa tshimbudzi
tsha tempile, nanena nai', Ngati uli Mwana wa Mulungu,
10 udziponye kuno: kuti alembedwa,

Adzauza anjelo atshi ndi iwe, ku sunga iwe:

11 ndi,

Pa manja ao adzatukula iwe,
Kani kapena udzagunda pazi lako pa mwala.

12 Ndimo Yesu kuiang'ka nanena nai', Anenedwa, Usayesa
Mwini Mulungu wako.

13 Ndimo ntawi diabolos anata zinyengo zonse, natshoka
kwa ie kwa ntawi.

14 Ndimo Yesu nabwera m' mpamvu ya Nzimu mwa Galile-
ya: ndimo mbiri nituruka ndi ie m' dziko lonse lozungulira.
15 Ndimo napunzitsa m' masinagoge ao, kupambanitsidwa ndi
onse.

16 Ndimo nafika kwa Nazarete, pomwe anakuliridwa: ndimo
naloa, monga mwambi watshi unali, m' sinagoge pa siku la
17 sabata, naima ku werenga. Ndimo linapatsidwa kwa ie
buku la mprofeti Yesaya. Ndimo natsegula buku, napeza
malo pomwe analembedwa,

18 Nzimu wa Mwini uli pa ine,
Tshifuka anadzosa ine ku uza ivangeli kwa osauka:
Wanditumiza ku uza kupulumutsa kwa mikoli,

Ndi kubwera kwa kuona kwa akungu,
Ku masula awo omwe azunzidwa,
Ku uza tshaka tshosekera tsha Mwini. 19
Ndimo natseka buku, nalipatsa anso ku woimirira, nakala 20
pansi: ndi maso a onse m' sinagoge anayang'anitsa ie.
Ndimo naiamba ku nena nao, Lero lemba limene ladzazidwa 21
m' makutu anu. Ndimo onse namariza nai', nazizwa ndi 22
mau a kufatsa omwe naturuka m' nkamwa mwatshi: ndimo
nati, Kodi amene sali mwana wa Yosefe? Ndimo nanena 23
nao, Mudzanena ndi ine nditu fanizo limene, Sing'anga,
udzitshiritse: zomwe tinamva zatshitidwa pa Kapernahum,
utshita anso kuno m' dziko lako. Ndimo nati, Dinena ndi inu 24
nditu, Palibe mprofeti alandiridwa m' dziko latshi. Koma 25
dinena ndi inu kwa nteradi, Amasie ambiri anali mwa
Sirayeli m' masiku a Eliya, ntawi mwamba munali motseka
dzaka dzitatu ndi miezi isanu ndi umodzi, ntawi tshaola
tshatshikuru tshinali m' dziko lonse; ndimo kwa palibe kwa 26
awo Eliya anatumidwa, koma woka kwa Tsarefate, m' dziko
la Tsidon, kwa nkazi emwe anali wamasie. Ndimo anali 27
ambiri akate m' Sirayeli m' ntawi ya Elishya mprofeti; ndi
palibe modzi wa awo anatsukidwa, koma Nahaman Msiriya
eka. Ndimo onse anadzazidwa ndi kukwiira m' sinagoge, 28
monga anamva zintu zimenezi; ndimo nauka, namturutsa 29
muzinda, namtsogoza ku phompo la piri pomwe mzinda
wao unamangidwa, kuti anangomponya ndi mutu. Koma 30
ie kupita pakati pa awo namuka.

Ndimo natsika kwa Kapernahum, mzinda wa Galileya. 31
Ndimo analikupunzitsa awo pa dzua la sabata: ndimo 32
nazizwa ndi kupunzitsa kwatshi; kuti mau atshi anali ndi
mpamvu. Ndimo m' sinagoge munali muntu, emwe anali 33
ndi nzimu wa demon wosatsuka; ndimo napfula ndi liu
lalikuru, A! tiri ndi tshiani ndi iwe, Yesu wa Nazarete? 34
kodi udza kutimwaza? dikudziwa iemwe uli, Woyera wa
Mulungu. Ndimo Yesu nasulumula ie, kuti, Tontola, ndimo 35
turuka kwa ie. Ndimo ntawi demon anamgwetsa pakati,
naturuka kwa ie, ndimo sanampweteketsa. Ndimo kuzizwa 36
kunali pa onse, nalankulana, modzi ndi wina, kuti, Mau
anje amenewa? kuti ndi kuweruza ndi mpamvu auza
mizimu yosatsuka, ndimo ituruka. Ndimo inaturuka mbiri 37
ya ie pa malo onse a dziko lozungulira.

Ndimo nauka ku sinagoge, naloa m' nyumba ya Simon. 38
Ndimo pongozi wa Simon nagwidwa ndi malungo akuru;

39 ndimo nampempa kwa ie. Ndimo naima pa ie, nasulumula
malungo; ndimo anatshoka *kwa* ie: ndimo tsopano lino
nauka naimirira kwa awo.
40 Ndimo ntawi dzua linalikuloa, onse awo omwe anali ndi
ena odwala ndi ntenda dzina natenga awa kwa ie; ndimo
41 naika manja atshi pa awo onse, natshiritsa awo. Ndimo
ademon anso naturuka mwa ambiri, kupfula, ndi kuti, Uli
Mwana wa Mulungu. Ndimo kusulumula awa, sanaletsa
awa ku lankula, tshifuka nadziwa kuti anali Kristu.
42 Ndimo ntawi kunali dzua, naturuka nang'ka m' tshipululu:
ndimo antu ambiri nafuna ie, nafika kwa ie, nafuna kumle-
43 tsa, kuti sakang'ka kwa awo. Koma nanena nao, Dikana-
uza ivangeli wa dziko la Mulungu kwa mizinda ina anso:
kuti kwa komwe dinatumidwa.
44 Ndimo analikuuza m' masinagoge a Galileya.
5 Ndimo kunali, ntawi antu ambiri natitimizana pa ie
namva mau a Mulungu, kuti analikuima mbali mwa nyanja
2 ya Genezarete; ndimo naona dzombo dziwiri dzirikuima
mbali mwa nyanja: koma apodzo anaturuka mwa idzo,
3 ndimo analikutsuka maukonde ao. Ndimo naloa m' tshi-
modzi tsha dzombo, tshomwe tshinali tsha Simon nafunsa ie
ku kang'ka pang'ono kuntunda. Ndimo nakala pansi napu-
4 nzitsa antu ambiri kwa tshombo. Ndimo ntawi naleka
kulankula, nanena ndi Simon, Kang'kirani kwa kuya, ndi
5 ponyani maukonde anu kwa kukoka. Ndimo Simon naiang'-
ka nanena, Ambuiye, tinagwira ntshito usiku wonse, ndimo
sitinagwira kantu: koma pa mau ako didzaponya maukonde.
6 Ndimo ntawi anatshita kumene, nakomaniza nsomba zambiri;
7 ndimo maukonde ao anatofuna ku ng'ambika; ndimo nako-
dola anzao m' tshombo tshina, kuti akadza ku tangata awa.
Ndimo nadza, nadzaza dzombo dziwiri, monga kuti dzinali-
8 kubira. Koma Simon Petros, ntawi nakuona, nagwa pa
maondo a Yesu, kuti, Tshoka kwa ine; kuti diri muntu
9 woipa, O Mwini. Kuti nazizwa, ndi onse omwe anali nai',
10 ndi kukoka kwa nsomba komwe anagwira; ndimo tshointsho
onso anali Yakobi ndi Yohane, ana a Zebediya, omwe anali
anzatshi a Simon. Ndimo Yesu nanena ndi Simon, Usaopa;
11 kwa ntawi yatsopano udzagwira antu. Ndimo ntawi ana-
tenga dzombo dzao pantunda, nasia zonse, namtsata.
12 Ndimo kunali, ntawi anali m' umodzi wa mizinda, ona,
muntu wodzaza ndi kate: ndimo ntawi naona Yesu, nagwa
pa nkope yatshi, napempa ie, kuti, Mwini, ngati ufuna,

udziwa kunditsuka. Ndimo naturutsa dzanja latshi, namtosa, 13
kuti, Difuna; utsukidwe. Ndimo tsopano lino kate lina-
tshoka kwa ie. Ndimo namuza sikuuza muntu modzi: 14
koma enda, nudzisonyeza kwa ndzukuru, nutsira kwa
kutsuka kwako, kofana Moses nauza, kwa kumariza ku awo.
Koma tshointsho tshambiri tshopambana inaturuka mbiri ya 15
ie: ndi antu ambiri nasong'kana ku mva, ndi ku tshiritsidwa
ndi mafoko ao. Koma nadzisunta ku dzipululu, na- 16
pempera.

Ndimo kunali pa limodzi la masiku amenewo, kuti anali- 17
kupunzitsa; ndimo analikukala pafupi Afarisi ndi apunzitsi
a mau, omwe naturuka midzi yonse ya Galileya ndi ya
Yudeya ndi Yerusalem: ndi mpamvu ya Mwini inali ndi ie
ku tshiritsa. Ndimo ona, amuna nanyamula pa kama 18
muntu iemwe wagwidwa ndi kunjenjemera: nafuna kumlo-
eza, ndimo kumika patsogolo pa ie. Ndimo sanapeza 19
bwanje anangomloeza tshifuka tsha antu ambiri, nakwera
pa mwamba pa nyumba, namtsitsa pakati pa mapale ndi
kama watshi mkati patsogolo pa Yesu. Ndimo kuona mvanu 20
wao, nati, Muntu zakwaipa zako zikululukidwa kwa iwe.
Ndimo akulembera ndi Afarisi naamba ku funsana, kuti, 21
Amene ali ndani, iemwe alankula matukwano? Ndani
adziwa ku kululukira zakwaipa, koma Mulungu eka?
Koma Yesu kudziwitsa maganizo ao, naiang'ka nanena nao, 22
Mufunsana tshiani m' mitima yanu? Tshiti tshiri tshope- 23
puka tshopambana, ku nena, Zakwaipa zako zikululukidwa
kwa iwe; kapena ku nena, Uka nuenda? Koma kuti 24
mudziwe kuti Mwana wa muntu ali ndi mpamvu pansi pano
ku kululukira zakwaipa (nanena ndi wodwala wonjenjemera),
Dinena ndi iwe, Uka, nutenga kama wako, numuka ku
nyumba yako. Ndimo tsopano lino nauka patsogolo pa 25
awo, natukula uyu pomwe nagona, namuka ku nyumba
yatshi, ku pambanitsa Mulungu. Ndimo kuzizwa kuna- 26
gwira onse, napambanitsa Mulungu; nadzazidwa ndi kuopa,
kuti, Taona zintu zozizwa lero.

Ndimo pambuiu pa zintu zimenezi naturuka, naona 27
wolandira tsong'ko, atshedwa Levi, kukala pa malo polandira
tsong'ko, nanena nai', Tsata ine. Ndimo nasia zonse, nauka 28
namtsata. Ndimo Levi nafotokozera ie kudia kwambiri m' 29
nyumba mwatshi: ndimo kunali antu ambiri a olandira
tsong'ko ndi a ena omwe anakala pa kudia ndi awo.
Ndimo Afarisi ndi akulembera ao nang'ung'udza pa akupu- 30

nzira atshi, kuti, Bwanje mudia ndi ku mwa ndi olandira
31 tsong'ko ndi ampulupulu? Ndimo Yesu kuiang'ka nanena
nao, Awo omwe ali olimba osali ndi kufunidwa ndi sing'-
32 anga; koma awo omwe ali odwala. Sindafika ku itana
33 odeka koma ampulupulu kwa kutembenuza ntima. Ndimo
nanena nai', Akupunzira a Yohane aleka kudia ntawi
zambiri, napanga mapempo; ndimo onso *akupunzira* a
34 Afarisi; koma ako adia ndi ku mwa. Ndimo Yesu nanena
nao, Kodi mudziwa ku panga mapungu ku leka kudia, ntawi
35 wokwati ali nao? Koma masiku adzadza; ndimo ntawi
wokwati adzatshotsedwa kwa awo, pomwe adzaleka kudia m'
36 masiku amenewo. Ndimo nanena nao onso fanizo; Palibe
muntu ang'amba tshigamba tsha maraia atsopano, natshiika
pa maraia akali; kani adzang'amba atsopano, ndimo onso
37 tshigamba tsha atsopano tshosadzafana ndi akali. Ndimo
palibe muntu atsira vinyo watsopano m' dzikopa dzakali;
kani, vinyo watsopano adzang'amba dzikopa, ndi adzatai-
38 kidwa, ndi dzikopa dzidzamwazika. Koma vinyo watsopano
39 akanaikidwa m' dzikopa dzatsopano. Ndimo palibe muntu
anamwa *vinyo* wakali, afuna watsopano: kuti ati, wakali ali
wabwino.

6 Ndimo kunali pa sabata, kuti analikupita pandule minda
ya dzintu; ndi akupunzira atshi nakadzula ngala za dzintu,
2 nadia, kusikisa izo m' manja ao. Koma ena a Afarisi nati,
Bwanje mutshita tshomwe sitshiri tshamau ku tshita pa siku
3 la sabata? Ndimo Yesu kuiang'ka awo nati, Kodi simuna-
werenga inde tshimenetshi, tshomwe Davide natshita, ntawi
4 anamva njala, ie, ndi awo omwe anali nai'; bwanje naloa
m' nyumba ya Mulungu, natenga nadia mikate yoonetsa,
napatsa anso ku awo omwe anali nai'; yomwe siiri yamau
5 ku dia koma kwa adzukuru oka? Nanena nao, Mwana wa
muntu ali mwini wa sabata.
6 Ndimo kunali pa sabata lina, kuti naloa m' sinagoge
napunzitsa: ndimo kunali muntu apo, ndi dzanja latshi
7 lamanja linauma. Ndimo akulembera ndi Afarisi nadikira
ie, ngati akatshiritsa pa sabata; kuti anangopeza bwanje ku
8 tshula ie. Koma nadziwa maganizo ao; ndimo nanena ndi
muntu emwe anali ndi dzanja latshi louma, Uka, ima uli pakati.
9 Ndimo nauka naima. Ndimo Yesu nanena nao, Dikufu-
nsani, Kodi kuli kwamau pa sabata ku tshita bwino, kapena
ku tshita koipa? ku pulumutsa moyo, kapena kuumwaza?
10 Ndimo nayang'anayang'ana pa awo onse, nanena nai',

Turutsa dzanja lako. Ndimo natshita *tshointsho:* ndimo
dzanja latshi linatshiritsidwa. Koma nakala ndi misala; 11
nauzana modzi ndi wina tshomwe anangotshita ndi Yesu.

Ndimo kunali m' masiku amene, kuti nang'ka ku piri ku 12
pempera; nakalabe usiku wonse m' kupempera kwa
Mulungu. Ndimo ntawi kunali dzua, naitana akupunzira 13
atshi: ndimo kwa awo nasang'ka kumi ndi awiri, omwe enso
natshedwa apostile; Simon, iemwe enso natshedwa Petros, 14
ndi Andreya mpwatshi, ndi Yakobi ndi Yohane, ndi Filipu
ndi Bartolomeyu, ndi Mateyu ndi Tomas, ndi Yakobi *mwana* 15
wa Alifeyu, ndi Simon emwe anatshedwa Zelote, ndi Yuda 16
*mwana* wa Yakobi, ndi Yuda Sikariyoti, iemwe anali nzondi;
ndimo natsika ndi awo, naima pa dambo, ndi antu ambiri a 17
akupunzira atshi, ndi antu ambiri kwa Yudeya lonse ndi
Yerusalem, ndi ku doko la Tire ndi Tsidon, omwe nadza ku
mva ie, ndi ku tshiritsidwa ndi ntenda zao; ndimo awo 18
omwe anapwetekedwa ndi mizimu yosatsuka natshiritsidwa.
Ndi antu ambiri onse nafuna ku tosa ie: kuti mpamvu 19
inaturuka mwa ie, ndimo inatshiritsa onse.

Ndimo natukula maso atshi pa akupunzira atshi, nati, 20
Odala *muli* inu osauka: kuti lanu liri dziko la Mulungu.
Odala *muli* inu nomwe mumva njala tsopano: kuti mu- 21
dzadzazidwa. Odala *muli* inu nomwe mulira tsopano: kuti
mudzaseka. Odala muli inu, ntawi antu adzakwiira inu, 22
ndimo ntawi adzagawa inu *kwa gulu lao*, nadzasautsa inu,
nadzaturutsa dzina lanu monga loipa, kwa Mwana wa muntu.
Sekerani m' dzua limene, ndimo lumpani *kwa tshimwemwe:* 23
kuti ona, sekeretso lanu liri lalikuru m' mwamba: kuti
tshointshi atatu ao natshita ndi aprofeti. Koma tshaipa 24
kwa inu nomwe muli olemera! kuti mwalandira kusanga-
latsa kwanu. Tshaipa kwa inu, inu nomwe muli odzaza 25
tsopano! kuti mudzamva njala. Tshaipa *kwa inu*, inu
nomwe museka tsopano! kuti mudzamva tshisoni ndi ku lira
nsozi. Tshaipa *kwa inu*, ntawi antu onse adzanena bwino 26
ndi inu! kuti tshointshi atatu ao natshita ndi aprofeti
onyenga.

Koma dinena ndi inu nomwe mumva, Kondani maliwongo 27
anu, tshitani bwino ndi awo omwe akwiira inu, dalani awo 28
omwe akutukwana inu, pemperani kwa awo omwe anyansa
inu. Kwa iemwe akumenya pa tsaia *limodzi* sonyeza anso lina; 29
ndimo kwa iemwe atshotsa tshopfundira tshako usakaniza
maraia ako onso. Patsa ku onse omwe afunsa iwe; ndi 30

31 kwa iemwe atshotsa zintu zako usazifunsa anso. Ndimo
monga mufuna kuti antu akatshita ndi inu, mutshite ku
32 awa anso modzimodzi. Ndimo ngati mukonda awo omwe
akonda inu, sekero lanje mupotshera? kuti inde ampulu-
33 pulu akonda awo omwe akonda awa. Ndimo ngati mutshita
bwino ndi awo omwe atshita bwino ndi inu, sekero lanje
mupotshera? kuti inde ampulupulu atshita modzimodzi.
34 Ndimo ngati mubwereka ku awo kwa omwe mulingalira
ku landira, sekero lanje mupotshera? inde ampulupulu
abwereka ku ampulupulu, ku landira modzimodzi inso.
35 Koma kondani maliwongo anu, ndimo tshitani bwino *nawo*,
ndimo bwerekani, palibe ntawi ku lizinga; ndimo sekeretso
lanu lidzakala lalikuru, ndimo mudzakala ana a Wopamba-
36 nitsa: kuti ali wokoma kwa osamika ndi oipa. Kalani inu
37 ndi nsisi, inde monga Atatu anu ali ndi nsisi. Ndimo
musaweruza, ndimo musadzaweruzidwa: ndimo musasutsa,
ndimo musadzasutsidwa: masulani, ndimo mudzamasulidwa:
38 patsani, ndimo tshidzapatsidwa kwa inu; kuyeza kwabwino,
kosindikiza, kosukisira, ndi kotula, adzapatsa inu m' dzifua
mwanu. Kuti ndi muyezo womwe muyeza udzayezedwa
kwa inu unso.

39 Ndimo nanena nao onso fanizo, Kodi akungu adziwa ku
tsogolera akungu? kodi sadzagwa awiri m' dzenje?
40 Wopunzira wosali wopambana mpunzitsi watshi: koma
onse ntawi anatetsedwa adzakala monga mpunzitsi wao.
41 Ndimo bwanje uona tshitolo tshomwe tshiri m' diso la
mbali wako, koma usaganiza ndi ntanda womwe uli m' diso
42 lako? Kapena bwanje udziwa ku nena ndi mbali wako,
Mbali, leka ine ku tshotsa tshitolo tshomwe tshiri m' diso
lako, ntawi iwe eka suona ntanda womwe uli m' diso lako?
Watshinyengo iwe, patsogolo tshotsa ntanda kwa diso lako,
ndimo pomwe udzaona bwino ku tshotsa tshitolo tshomwe
43 tshiri m' diso la mbali wako. Kuti palibe ntengo wabwino
womwe ubala dzobala dzobvunda; kapena anso ntengo wo-
44 bvunda womwe ubala dzobala dzabwino. Kuti mitengo
yonse idziwidwa ndi dzobala dza iyo. Kuti kwa minga
antu osakung'kha zinkhuyu, kapena kwa tshifutu tsha
45 ntungwi osakung'kha magrepe. Muntu wabwino kwa
kulemera kwabwino kwa ntima watshi aturutsa tshomwe
tshiri tshabwino; ndi *muntu* woipa kwa *kulemera* koipa
aturutsa tshomwe tshiri tshoipa: kuti kwa kutshuruka kwa
ntima, nkamwa mwatshi mulankula.

Ndimo bwanje mutsha ine, Mwini, Mwini, ndimo 46
musatshita zintu zomwe dinena? Iemwe adza kwa ine, 47
namva mau anga, naatshita didzasonyeza inu ku emwe ali
wofana: ali wofana ndi muntu kumanga nyumba, emwe 48
nakumba kuya, nazika pa tantwe: ndimo ntawi tshigumula
tshinauka, ntsinje unamenya pa nyumba imeneyo, ndimo
usanadziwa kuigwedeza: tshifuka kuti inamangidwa bwino.
Koma iemwe amva, ndimo wosatshita, ali wofana ndi muntu 49
iemwe namanga nyumba pa ntaka yopanda kuzika; pa
yomwe ntsinje unamenya, ndimo tsopano lino inagwa
mbwalo; ndi kupasuka kwa nyumba imene kunali
kwakukuru.

Pambuiu anata kunena kwatshi konse m' makutu a antu, 7
naloa m' Kapernahum.

Ndimo kapolo wa kenturione modzi, emwe anakondedwa 2
ndi ie, anadwala, nafuna ku fa. Ndimo ntawi anamva ndi 3
Yesu, natumiza kwa ie akuru a Ayuda, kufunsa ie kuti
akadza nakapulumutsa kapolo watshi. Ndimo awo, ntawi 4
anadza kwa Yesu, napempa ie kolimba, kuti, Ali woenera
kuti ukatshita tshimenetshi kwa ie: kuti akonda mtundu 5
watu, ndimo ie eka anamanga kwa ife sinagoge latu.
Ndimo Yesu namuka nao. Ndimo ntawi tsopano anali si 6
kutali kwa nyumba, kenturione natumiza abali kwa ie,
kunena ndi ie, Mwini, usaśautsa iwe eka: kuti sindiri
woenera kuti ukaloa pansi pa tshindu langa: mwa kuti 7
kapena sindinaganiza ine ndeka woenera ku fika kwa iwe:
koma nena mau, ndimo mwana wanga adzatshiritsidwa.
Kuti diri inso mamuna kuikidwa pansi pa kuweruza, kupo- 8
tshera pansi pa ine ankhondo: ndimo dinena ndi amene,
Muka, ndimo amuka; ndimo kwa wina, Idza, ndimo adza;
ndi kwa kapolo wanga, Tshita tshimenetshi, ndimo atshi-
tshita. Ndimo ntawi Yesu anamva zintu zimenezi, nazi- 9
zwa ndi ie, natembenuka nanena ndi antu ambiri omwe
anatsata ie, Dinena ndi inu, Sindinapeza mvanu woukuru
tshointshi, iai, si mwa Sirayeli. Ndimo awo omwe anatu- 10
midwa, ku bwera ku nyumba, napeza kapolo wolimba.

Ndimo kunali nsanga pambuiu, kuti namuka ku mzinda 11
utshedwa Nayin; ndi akupunzira atshi nang'ka nai', ndi
antu ambiri. Ndimo ntawi nayandika ndi tshipata tsha 12
mzinda, ona, kunanyamulidwa kunja modzi emwe anafa,
mwana modzi wa amai atshi, ndimo ie anali wamasie: ndi
antu ambiri a mzinda anali nai'. Ndimo ntawi Mwini 13

namona, nakala ndi tshisoni nai', nanena nai', Usalira.
14 Ndimo nayandika natosa tshitanda: ndimo akunyamula
naima. Ndimo nati, Nyamata, dinena ndi iwe, Uka.
15 Ndimo wakufa nauka, naamba ku lankula. Ndimo napatsa
16 ie ku amai atshi. Ndimo kuopa kunagwira onse: ndimo
napambanitsa Mulungu, kunena kuti, Mprofeti wang'kuru
anauka mwa ife: ndimo kuti, Mulungu anatsheza ndi antu
17 atshi. Ndimo mbiri imene inaturuka ndi ie m' Yudeya
lonse, ndi dziko lonse lozungulira.
18 Ndimo akupunzira a Yohane namsonyeza ndi zintu zonse
19 zimenezi. Ndimo Yohane kuitana kwa ie awiri a akupu-
nzira atshi natumiza awa ku Mwini, kuti, Kodi uli iemwe
20 alikufika, kapena tiyang'anire wina? Ndimo ntawi antu
anafika kwa ie, nanena, Yohane Mbapatizi anatumiza ife
kwa iwe, kuti, Kodi uli iemwe alikufika, kapena tiyang'a-
21 nire wina? Ndimo mwa ora lomwe natshiritsa ambiri kwa
zintenda ndi kwa miliri ndi kwa mizimu yoipa; ndi kwa
22 ambiri akungu napatsa kuona. Ndimo naiang'ka nanena
nao, Mukani, uzani Yohane zintu zomwe munaziona ndi
munazimva; akungu alandira kuona kwao, opunduka
miendo aenda, akate atsukidwa, ndi ogonta amva, akufa
23 adzukitswa, osauka auzidwa ivangeli. Ndimo wodala ali
ie, emwe wosadzakwiitsidwa ndi ine.
24 Ndimo ntawi mitenga ya Yohane inatshoka, naamba ku
nena ndi antu ambiri ndi Yohane, Munang'ka m' tshipululu
ku ona tshiani? nzengo inagwedezedwa ndi mpepo kodi?
25 Koma munaturuka ku ona tshiani? muntu anabvala nsaru
zofewa? Onani, awo omwe abvala nsaru zolemera, naeta
26 zintu zabwino, ali m' malo a mafumu otshuka. Koma
munaturuka ku ona tshiani? mprofeti? Inde, dinena ndi
27 inu, ndi wambiri wopambana mprofeti. Amene ali ie wa
iemwe tshilembedwa,

Ona ditumiza ntenga wanga patsogolo pa nkope yako,
Iemwe adzakonzetsa njira yako patsogolo pa iwe.

28 Dinena ndi inu, Mwa awo omwe abadwa ndi akazi wosali
modzi wang'kuru wopambana Yohane: koma iemwe ali
wang'ono wopambana m' dziko la Mulungu ali wang'kuru
29 wopambana ie. Ndimo antu onse ntawi anamva, ndi
olandira tsong'ko, nadeketsa Mulungu, kunabapatizidwa ndi
30 bapatisma la Yohane. Koma Afarisi ndi ankoswe nataia
kwa awo oka kwiyeruza kwa Mulungu, sikunabapatizidwa
31 ndi ie. Ndimo ndi tshiani didzafaniza antu a fuko limeneli,

ndi kwa tshiani ali ofana? Ali ofana ndi ana omwe akala 32
m' malo a maronda, naitana modzi kwa wina; omwe ati,
Tinaomba milumbwi kwa inu, ndimo musanabvina; tina-
pfula, ndimo musanalira nsozi. Kuti Yohane Mbapatizi 33
anadza sanadia nkate kapena sanamwa vinyo; ndimo muti,
Apotshera demon. Mwana wa muntu anafika kudia ndi 34
kumwa; ndimo munena, Ona, muntu wosusuka, ndi
wakumwa vinyo, mbali wa olandira tsong'ko ndi ampulu-
pulu! Ndimo nzeru ideketsedwa ndi ana atshi 35
onse.

Ndimo modzi wa Afarisi nafuna ie kuti akadia nai'. 36
Ndimo naloa m' nyumba ya Mfarisi, nakala pa kudia.
Ndimo ona, nkazi emwe anali muzinda, wampulupulu; 37
ndimo ntawi nadziwa kuti analikukala pa kudia m' nyumba
ya Mfarisi, natenga nsupa ya alabastile ya mafuta, ndimo 38
kuima pambuiu pa mapazi atshi, kulira nsozi, naamba ku
katamiza mapazi atshi ndi misozi yatshi, napukuta awa ndi
tsisi la mutu watshi, namsomsona mapazi atshi, nadzosa awo
ndi mafuta. Ndimo ntawi Mfarisi iemwe anaitana ie naona, 39
nanena mwa ie eka, kuti, Muntu amene, ngati anali
mprofeti, akanadziwa ndani ndi wanje nkazi amene ali emwe
atosa ie, kuti ali wampulupulu. Ndimo Yesu kuiang'ka 40
nanena nai', Simon, diri ndi kantu ku nena ndi iwe.
Ndimo ati, Mpunzitsi, nena. Wagongole modzi anali ndi 41
amangawa awiri: modzi wakong'gola madenariyon madzana
asanu, ndi wina makumi asanu. Ndimo ntawi analibe 42
*kantu* ku lipira, nakulululukira awa awiri. Ndimo uti wa
awa adzakonda ie kopambana? Simon naiang'ka nati, Ie, 43
diganiza, kwa emwe nakulululukira kopambana. Ndimo
nanena nai', Waweruza bwino. Ndimo kutembenuka kwa 44
nkazi, nanena ndi Simon, Kodi uona nkazi amene? Daloa
m' nyumba yako, sunapatsa ine madzi kwa mapazi anga:
koma ie anakatamiza mapazi anga ndi misozi yatshi, napu-
kuta awo ndi tsisi latshi. Sunapatsa ine kumsomsona: 45
koma ie, kwa ntawi daloa, sanaleka ku somsona mapazi anga.
Mutu wanga ndi mafuta sunadzosa: koma ie wadzosa 46
mapazi anga ndi mafuta. Ndimo dinena ndi iwe, Zakwaipa 47
zatshi, zomwe ziri zambiri, zikulululukidwa; kuti nakonda
kwambiri: koma ku iemwe kang'ono kakulululukidwa, *iemwe*
akonda kang'ono. Ndimo nanena nai', Zakwaipa zako 48
zikulululukidwa. Ndimo awo omwe anakala pa kudia ndi ie 49
naamba ku nena mwa iwo oka, Ndani ali amene iemwe inde

50 akululukira zakwaipa? Ndimo nanena ndi nkazi, Mvanu
wako wapulumutsa iwe; muka ndi ntendere.
8 Ndimo kunali nsanga pambuiu, kuti nang'ka m' mizinda
ndi m' midzi, kuuza ndi kutenga ivangeli wa dziko la
2 Mulungu, ndimo ndi ie kumi ndi awiri, ndi akazi ena omwe
anatshiritsidwa ndi mizimu yoipa ndi mafoko, Mariya emwe
natshedwa kwa Magadala, mwa emwe naturuka ademon
3 asanu ndi awiri, ndi Yohana nkazi wa Kuza ndindo wa
Herode, ndi Susana, ndi ena ambiri, omwe naimirira kwa
awo ndi zintu zao.
4 Ndimo ntawi antu ambiri anasong'kana, ndimo awo a
5 mizinda yonse nafika kwa ie, nanena ndi fanizo: Wofesa
naturuka ku fesa mbeu yatshi: ndimo monga analikufesa,
ina inagwa mbali mwa njira; ndimo inapondedwa, ndi
6 mbalame za mlengalenga zinaidia. Ndimo ina inagwa pa
tantwe; ndimo nsanga monga inamera, inanyala, tshifuka
7 inakala yopanda nyonto. Ndimo ina inagwa pakati pa
minga; ndi minga inamera naiyo, ndimo inaikwinyatitsa.
8 Ndimo ina inagwa pa ntaka yabwino, ndimo inamera, ndimo
inabala dzobala dzatshi makumi okaoka kumi. Monga
ananena zintu zimenezi, napfula, Iemwe ali makutu ku mva,
amve.
9 Ndimo akupunzira atshi namfunsa fanizo limene linango-
10 kala bwanje. Ndimo nati, Kwa inu kupatsidwa ku dziwa
zosadziwika za dziko la Mulungu: koma kwa ena m'
mafanizo; kuti kuona osangoona, ndi kumva osangomvetsa.
11 Ndimo fanizo liri limeneli: Mbeu iri mau a Mulungu.
12 Ndi amene mbali mwa njira ali omwe anamva; ndimo
diabolos adza, natshotsa mau kwa mitima yao, kuti sangoa-
13 mvana ndi ku pulumutsidwa. Ndimo amene pa tantwe *ali*
awo omwe, ntawi anamva, alandira mau ndi tshimwemwe;
ndi amene ali opanda ntsitsi, omwe kwa ntawi amvana,
14 ndimo pa ntawi ya tshinyengo aleka. Ndi imene yomwe
inagwa mwa minga, amene ali awo omwe anamva, ndi
monga analikupita nakwinyatitswa ndi zisoni ndi zolemera
ndi masekeretso a moyo *umene*, ndimo osabala dzobala
15 dzopsa dzabwino. Ndimo imene pa ntaka yabwino, amene
ali otere monga mutima wosaba ndi wabwino, anamva mau,
asunga kolimba, nabala dzobala ndi kulongosoka.
16 Ndimo palibe muntu, ntawi waatsa muni, avundikila uo
ndi tshiwira, kapena auika pansi pa kama; koma auika pa
17 tshogwirira, kuti omwe aloa angoona kuunika. Kuti kulibe

kantu kobisidwa, komwe kosadzasonyezedwa; kapena *kantu*
kakutseri, komwe kosadzadziwidwa ndi kadzaturukira
poyera. Ndimo yang'anirani bwanje mumva: kuti iemwe 18
apotshera, kwa ie adzapatsidwa; ndi emwe wosapotshera,
kwa ie adzatshotsedwa inde tshomwe aganiza apotshera.

Ndimo nafika kwa ie amai atshi ndi abali atshi, ndimo 19
sanadziwa kumwandika tshifuka tsha antu ambiri. Ndimo 20
tshauzidwa ie, Amai ako ndi abali ako aima kunja, kufuna
ku ona iwe. Koma naiang'ka nanena nao, amai anga ndi 21
abali anga ali amene omwe amva mau a Mulungu, naatshita.

Ndimo kunali pa limodzi la masiku amenewo, kuti naloa 22
m' tshombo, ie eka ndi akupunzira atshi; ndimo nanena nao,
Tiyambuke patsidia lina la nyanja: ndimo nakang'ka.
Koma monga analikupita ndi matanga nagona: ndimo 23
unatsika mondwe wa mpepo pa nyanja; ndimo analikudzaza
*ndi madzi*, nakala ndi madzidzi. Ndimo nafika kwa ie, 24
nadzutsa ie, kuti, Ambuiye, ambuiye, timwazika. Ndimo
nadzuka, nasulumula mpepo ndi kukwia kwa madzi: ndimo
zinaleka, ndimo kunali bata. Ndimo nanena nao, Mvanu 25
wanu uli kuti? Ndimo kuopa nazizwa, kuti modzi ndi
wina, Ndimo amene ali ani, kuti auza inde mpepo ndi madzi,
ndimo zimvera ie?

Ndimo nafika pa dziko la Agerasa, lomwe liri pandunji 26
ndi Galileya. Ndimo ntawi naturuka pa ntunda, nakomana 27
ndi ie ku mzinda muntu modzi, emwe anapotshera ademon;
ndi kwa ntawi yambiri sanabvala nsaru, ndi sanakala m'
nyumba *imodzi*, koma m' mianda. Ndimo ntawi naona 28
Yesu, napfula, nagwa patsogolo pa ie, ndi liu lalikuru wati,
Dirikutshita tshiani ndi iwe Yesu iwe Mwana wa Mulungu
Wopambanitsa? Dipempa iwe, usandizunze. Kuti anauza 29
nzimu wosatsuka ku turuka kwa muntu. Kuti ntawi
zambiri unagwira ie: ndimo nadikiridwa, namangidwa ndi
maunyolo ndi magrigadyera; ndimo kudula zomangira,
natsogozwa ndi demon m' dzipululu. Ndimo Yesu namfunsa, 30
Dzina lako liri lani? Ndimo nati, Lijon; kuti ademon
ambiri analoa mwa ie. Ndimo namfunsa kuti sakauza awa 31
ku turuka mwa mphompo. Ndimo linali apo gulu la 32
nkhumba zambiri kueta pa piri: ndimo nafunsa ie kuti
akaloleza awo ku loa mwa izo. Ndimo naloleza. Ndimo 33
ademon naturuka kwa muntu, naloa mwa nkhumba: ndimo
gulu linatsika nsanga malo otseruka m' nyanja, natseka
pwea. Ndimo ntawi omwe naeta izo naona tshomwe 34

35 tshinali, natawa, nauza m' mzinda ndi m' minda. Ndimo
naturuka ku ona tshomwe tshinali; ndimo nafika kwa
Yesu, napeza muntu, mwa emwe ademon anatshoka, kukala,
nabvala, ndi nzeru zatshi zabwino, pa mapazi a Yesu: ndimo
36 anaopa. Ndimo awa omwe anatshiona nauza awa bwanje
37 iemwe anagwidwa ndi ademon anatshiritsidwa. Ndimo
antu onse a dziko la Agerasa lozungulira napempa ie ku
tshoka kwa awa; kuti nagwidwa ndi kuopa kwambiri:
38 ndimo naloa m' tshombo, nabwera. Koma muntu mwa
emwe ademon anaturuka napempera ie kuti anangokala
39 nai': koma namtshotsa, kuti, Bwera ku nyumba yako,
nusonyeza bwanje zintu zazikuru Mulungu anatshita kwa
iwe. Ndimo namuka, ku uza muzinda wonse bwanje zintu
zazikuru Yesu anatshita nai'.

40 Ndimo monga Yesu nabwera, antu ambiri nalandira ie
41 ndi kusekera; kuti onse analikulindira ie. Ndimo ona,
nafika muntu atshedwa Yayiro, ndimo anali mkuru wa
sinagoge: ndimo nagwa pa mapazi a Yesu, napempa ie ku
42 loa m' nyumba yatshi; kuti anali ndi butu limodzi loka,
linali ndi dzaka kumi ndi dziwiri, ndimo linagona linafuna
ku fa. Koma monga analikupita antu ambiri naunjikana
pa ie.

43 Ndimo nkazi anali ndi kuka mwazi dzaka kumi ndi
dziwiri, emwe anata zomwe anali nazo kwa asing'anga,
44 ndimo sanadziwa ku tshiritsidwa ndi wina, nadza pambuiu
pa ie, natosa mtsheu wa mwinjiro watshi: ndimo tsopano
45 lino kuka kwa mwazi watshi kwaleka. Ndimo Yesu wati,
Wanditosa ndani? Ndimo ntawi onse nakana, Petros
nanena, ndi awa omwe anali nai', Ambuiye, antu ambiri
46 aunjikana pa iwe natitimiza *iwe.* Koma Yesu wati, Wina
wanditosa: kuti dinadziwitsa kuti mpamvu yaturuka kwa
47 ine. Ndimo ntawi nkazi naona kuti sanabisidwa, nadza ndi
kuntentemera, ndimo kugwa patsogolo pa ie nauza patsogolo
pa antu onse kwa tshifukwa tshanje anatosa ie, ndimo
48 bwanje anatshiritsidwa tsopano lino. Ndimo nanena nai',
Mwana wankazi, mvanu wako wakutshiritsa; enda ndi
ntendere.

49 Ntawi analikulankula, afika modzi ku *nyumba* ya mkuru
wa sinagoge, kuti, Butu lako lafa; leka nkhani Mpunzitsi.
50 Koma Yesu analikumva, naiang'ka ie, Usaopa: mvana
51 koka, ndimo lidzatshiritsidwa. Ndimo ntawi nafika ku
nyumba, naletsa, muntu palibe ku loa ndi ie, koma Petros,

ndi Yohane, ndi Yakobi, ndi atatu atshi ndi amai atshi a
butu. Ndimo onse analikulira nsozi, ndi kupfulira ie: 52
koma nati, Musalira nsozi; kuti sanafa, koma ligona. Ndimo 53
naseka ie kwambiri, kudziwa kuti linafa. Koma ie, kutenga 54
ilo ndi dzanja, naitana, kuti, Butu, uka. Ndimo nzimu 55
watshi unabwera, ndimo linauka nsanga: nauza ku patsa
ilo ku dia. Ndimo atatu atshi ndi amai atshi nazizwa: 56
koma nauza awa sikuuza muntu ndi tshomwe tshinatshi-
tidwa.

Ndimo nasong'kanitsa kumi ndi awiri, napatsa awa 9
mpamvu ndi kuweruza pa ademon onse, ndi ku tshiritsa
zintenda. Ndimo natumiza awa ku uza dziko la Mulungu, 2
ndi ku tshiritsa odwala. Ndimo nanena nao, Musatenga 3
kantu kwa ulendo wanu, kapena ndodo, kapena katumba,
kapena nkate, kapena ndrama; kapena musapotshera miinji-
ro iwiri. Ndi m' nyumba yomwe muloa, kalani apo, ndimo 4
apo mumuka. Ndimo monga ambiri monga osafuna ku 5
landira inu, ntawi muturuka muzinda umene, sansani fumbi
kwa mapazi anu kwa kumariza pa awo. Ndimo namuka, 6
napita m' mizinda, kuuza ivangeli, ndi kutshiritsa m' malo
onse.

Ndimo Herode woweruza wa tshinai anamva ndi zonse 7
zomwe zinatshitidwa: nasautswa kwambiri, tshifuka kuti
ananenedwa ndi ena, kuti Yohane anaukitswa kwa akufa;
ndimo ndi ena, kuti Eliya anasonyeza; ndimo ndi ena, kuti 8
modzi wa aprofeti akali anaukitswa anso. Ndimo Herode 9
nati, Yohane dinadula mutu: koma amene ali ani, ndi
emwe dimva zintu zotere? Ndimo nafuna ku ona ie.

Ndimo apostile, ntawi anabwera, nauza ie zintu zomwe 10
anazitshita. Ndimo natenga awa, nang'ka kutseri ku mzinda
utshedwa Betsayida. Koma antu ambiri kudziwitsa na- 11
mtsata; ndimo nalandira awo ndi kusekera, nalankula nao
ndi dziko la Mulungu, ndi awo omwe anali ndi kufunidwa
ndi kutshiritswa, natshiritsa. Ndimo dzua linalikupita; 12
ndimo kumi ndi awiri nadza, nanena nai', Tshotsa antu
ambiri, kuti angoenda m' midzi ndi m' dziko lozungulira,
ku gona, nalandira kudia: kuti pano tiri m' malo atshipu-
lulu. Koma nanena nao, Patsani awa ku dia. Ndimo 13
nati, Tiribe kantu kopambana mikate isanu ndi nsomba
ziwiri; kani tikaenda ku gula kudia kwa antu onse amene.
Kuti anali amuna kwa mazousan asanu. Ndimo nanena 14
ndi akupunzira atshi, Pangani awo ku kala pansi m' magulu,

15 ndi kwa makumi asanu pa limodzi. Ndimo natshita tshoi-
16 ntsho, napanga awo onse ku kala pansi. Ndimo natenga
mikate isanu ndi nsomba ziwiri, nayang'ana ku mwamba,
nadalitsa izo, naswa; napatsa ku akupunzira ku ika patso-
17 golo pa antu ambiri. Ndimo nadia, nakuta onse: ndimo
kunatoledwa zomwe zinatsala ku awo za nyenyeswa, mitanga
kumi ndi iwiri.
18 Ndimo kunali, monga anali eka kupempera, akupunzira
anali nai': ndimo nafunsa awa, kuti, Antu ambiri anena
19 kuti diri ani? Ndimo awo kuiang'ka nati, Yohane Mbapa-
tizi; koma ena, Eliya; ndi ena, kuti modzi wa aprofeti
20 akali aukitswa anso. Ndimo nanena nao, Koma munena
kuti diri ani? Ndimo Petros kuiang'ka nati, Kristu wa
21 Mulungu. Koma nanena nao, nauza *awa* siauza muntu
22 tshimenetshi; kuti, Mwana wa muntu akanamva zintu
zambiri, ndi akanakanidwa ndi akuru ndi adzukuru akuru
ndi akulembera, ndi akanapedwa, ndi pa dzua latshitatu
23 akanaukitswa. Ndimo nanena ndi onse, Ngati muntu modzi
afuna ku tsata pambuiu pa ine, leka ie ku dzikana, ndi ku
24 tukula nkhwitshi yatshi masiku onse, nanditsata. Kuti
iemwe afuna ku pulumutsa moyo watshi adzaumwaza; koma
iemwe adzamwaza moyo watshi kwa ine, iemwe adzaupulu-
25 mutsa. Kuti, muntu apindulidwa bwanje, ngati apeza
dziko lonse, nadzimwaza ie eka kapena ku tshotsedwa?
26 Kuti iemwe adzakala ndi manyazi, tshifuka tsha ine ndi tsha
mau anga, ndi ie Mwana wa muntu adzakala ndi manyazi,
ntawi adza m' kupambana kwatshi, ndi *kupambana* kwa
27 Atate, ndi kwa anjelo oyera. Koma dinena ndi inu kwa
nteradi, Alipo ena a awo omwe aima pano, omwe sadzalawa
nditu ndi imfa, kwa ntawi aona dziko la Mulungu.
28 Ndimo kunali pa masiku asanu ndi atatu pambuiu mau
amene, natenga nai' Petros ndi Yohane ndi Yakobi, nakwera
29 pa piri ku pempera. Ndimo monga analikupempera, maka-
lidwe a nkope yatshi anasandulizidwa, ndi nsaru zatshi
30 *zinali* zoyera *ndi* zowala. Ndimo ona, analankula ndi ie
31 antu awiri, omwe anali Moses ndi Eliya; omwe nasonyeza
m' kupambana, nanena ndi imfa yatshi yomwe anatofuna
32 ku ta pa Yerusalem. Koma Petros ndi awo omwe anali nai'
analemedwa ndi ntulo: koma ntawi anali maso nditu, naona
kupambana kwatshi, ndi antu awiri omwe naima ndi ie.
33 Ndimo kunali, monga analikumuka kwa ie, Petros nanena
ndi Yesu, Ambuiye, tshiri tshabwino kwa ife tiri pano;

ndimo timange masasa atatu; limodzi kwa iwe, ndi limodzi
kwa Moses, ndi limodzi kwa Eliya: siadziwa tshomwe
nanena. Ndimo ntawi nanena zintu zimenezi, unadza 34
ntambo, ndimo unatsita awo: ndimo naopa monga naloa
muntambo. Ndimo liu linaturuka muntambo, kuti, Amene 35
ali Mwana wanga, wosang'kidwa wanga: imvani ie. Ndimo 36
ntawi liu linadza, Yesu anapezedwa eka. Ndimo natontola,
ndimo sanauza muntu m' masiku amenewo zina za zintu
zomwe anaziona.

Ndimo kunali, pa mawa, ntawi anatsika pa piri, antu 37
ambiri nakomana ndi ie. Ndimo ona, muntu kwa antu 38
ambiri napfula, kuti, Mpunzitsi, dipempa iwe ku yang'anira
mwana wanga; kuti ali mwana wanga modzi: ndimo ona, 39
nzimu ugwira ie, ndimo apfula kwansangu; ndimo upweteketsa
ie kuti akala ndi povu, ndimo kolimbika uleka ie, kutundudza
ie kwambiri. Ndimo dinapempa akupunzira ako ku turutsa 40
iwo; ndimo sanadziwa *ku tshita.* Ndimo Yesu naiang'ka 41
nati, O fuko lopanda mvanu ndi losasamala, ntawi ingati
didzakala ndi inu, ndimo didzalola inu? tenga mwana wako
kuno. Ndimo monga analinkudza kosuntira, demon na- 42
mgwetsa pansi, na*m*pweteketsa kwambiri. Koma Yesu
nadzudzula nzimu wosatsuka, natshiritsa mwana, nambweza
ku atatu atshi. Ndimo onse nazizwa ndi ukuru wa 43
Mulungu.

Koma ntawi onse analikuzizwa ndi zintu zonse zomwe
natshita, nanena ndi akupunzira atshi, Lekani mau amene 44
ku bira m' makutu mwanu: kuti Mwana wa muntu adza-
perekedwa m' manja mwa antu. Koma sanadziwika ku 45
nena kumene, ndimo kunabisidwa kwa awo, kuti sakaonetsa:
ndimo naopa kumfunsa ndi kunena kumene.

Ndimo kunauka kuuzana mwa awo, ndani wa awo akakala 46
wang'kuru. Koma Yesu kuonetsa ganizo la mitima yao, 47
natenga kamwana, nakaika pa kundu patshi, nanena nao, 48
Iemwe adzalandira kamwana kamene m' dzina langa
alandira ine: ndi iemwe adzalandira ine, alandira iemwe
ananditumiza: kuti iemwe ali wang'ono mwa inu nonse,
iemwe akala wang'kuru.

Ndimo Yohane naiang'ka nati, Ambuiye tinaona modzi 49
kuturutsa ademon m' dzina lako; ndimo tinamletsa, tshi-
fuka wosatsatana ndi ife. Koma Yesu nanena nai', Usa- 50
*m*letsa: kuti iemwe wosali pa inu ali ndi inu.

Ndimo kunali, ntawi masiku analikukwanira kuti akana- 51

landiridwa kumwamba, naika kolimbika nkope yatshi ku
52 muka ku Yerusalem, ndimo natumiza mitenga patsogolo pa
nkope yatshi: ndimo namuka, naloa m' mudzi wa Asamariya,
53 ku konzetsa kwa ie. Ndimo sanalandira ie, tshifuka nkope
yatshi inali *monga ngati nafuna* ku ng'ka kwa Yerusalem.
54 Ndimo ntawi akupunzira atshi Yakobi ndi Yohane anaona
*tshimenetshi*, nati, Mwini, kodi ufuna kuti tiuze moto ku
55 tsika kwa kumwamba, ku otsha awa? Koma natem-
56 benuka, nadzudzula awo. Ndimo namuka ku mudzi wina.
57 Ndimo monga napita pa njira, muntu modzi nanena nai',
58 Didzatsata iwe pomwe umuka. Ndimo Yesu nanena nai',
Ankhandwe ali ndi mapanga, ndi mbalame za mlengalenga
*ziri ndi* dzisa: koma Mwana wa muntu wosapotshera malo
59 ku ika mutu watshi. Ndimo nanena ndi wina, Tsata ine.
Koma nati, Mwini, leka ine patsogolo ku ng'ka ku ika atatu
60 anga m' mwanda. Koma nanena nai', Leka akufa ku ika
akufa ao m' mwanda; koma muka iwe nubukitsa dziko la
61 Mulungu. Ndimo wina anso nati, Didzatsata iwe, Mwini;
koma leka ine patsogolo ku tsazika awo omwe ali ku
62 nyumba yanga. Koma Yesu nanena nai', Palibe muntu,
waika dzanja latshi pa tshokoketsa, nayang'ana kumbuiu,
ali woenera kwa dziko la Mulungu.

10 Ndimo pambuiu pa zintu zimenezi Mwini naloeza
makumi asanu ndi awiri ena, ndimo natumiza awo awiri
ndi awiri patsogolo pa nkope yatshi m' mizinda yonse ndi
2 m' malo onse, pomwe ie eka anafuna ku fika. Ndimo
nanena nao, Masika ali otshuruka, koma antshito ali
owereng'jeka: ndimo pemperani Mwini wa masika, kuti
3 atumize antshito mwa masika atshi. Mukani: ona, ditu-
4 miza inu monga ana a nkosa pakati pa zirombo. Musanya-
mula kapena katumba, kapena tumba, kapena zikwakwata:
5 ndimo musautsa muntu pa njira. Ndimo m' nyumba
yomwe mudzaloa, pakuamba mudzanena, Ntendere ukale pa
6 nyumba imene. Ndimo ngati mwana wa ntendere ali apo,
ntendere wanu udzakala pa ie: koma ngati iai, udzate-
7 mbenuka anso kwa inu. Ndimo m' nyumba yomwe kalani,
kudia ndi kumwa zintu zomwe monga apatsa: kuti wan-
tshito ali woenera kwa kulipira kwatshi. Musamuka ku
8 nyumba ndi nyumba. Ndimo muzinda womwe muloa,
ndimo alandira inu, idiani zintu zotere monga ziikidwa
9 patsogolo pa inu: ndimo tshiritsani odwala omwe ali mo-
mo, ndimo munena nao, Dziko la Mulungu laandika ndi

inu. Koma muzinda womwe mudzaloa, ndimo osalandira 10
inu, mukani m' makwalala a iwo ndimo munena, Inde 11
fumbi la mzinda wanu, lomwe likala pa mapazi atu, tipu-
kutira pa inu: koma dziwani tshimene, kuti dziko la
Mulungu laandika. Dinena ndi inu, kudzamva pang'ono 12
m' siku lidya kwa Sodom, kopambana mzinda udya.
Tshaipa kwa iwe, Korazin! tshaipa kwa iwe, Betsayida! 13
kuti ngati mpamvu zinatshitidwa m' Tire ndi m' Tsidon,
zomwe zinatshitidwa mwa inu, kali akanatembenuza mitima
yao, kukala ndi tshiguduli ndi mapolusa. Koma kudzali 14
kumva pang'ono kwa Tire ndi Tsidon m' kuweruza, ndi kwa
inu. Ndi iwe, Kapernahum, kodi udzakulitsidwa ku 15
mwamba? udzatsitsidwa kwa Hadesi. Iemwe amva inu, 16
amva ine; ndi iemwe anyadira inu anyadira ine;
ndi iemwe anyadira ine anyadira iemwe ananditu-
miza.

Ndimo makumi asanu ndi awiri nabwera ndi kusekera, 17
kuti, Mwini, inde ademon ali pansi pa ife mwa dzina lako.
Ndimo nanena nao, Daona Satana kugwa monga mpezi kwa 18
kumwamba. Ona, dapatsa inu mpamvu ku ponda zinjoka 19
ndi zinkanira, ndi pa mpamvu yonse ya liwongo: ndi palibe
kantu nditu kadzapweteketsa inu. Koma musasekera ndi 20
tshimene, kuti mizimu iri pansi pa inu; koma sekerani kuti
maina anu alembedwa kumwamba.

Mwa ora limene nasekera m' Nzimu Woyera, nati, 21
Diamika iwe, O Atate, Mwini wa kumwamba ndi pansi,
kuti unabisa zintu zimenezi kwa anzeru ndi kwa odziwa,
ndimo unazisonyeza ku makanda: inde, Atate; kuti
tshointsho kunali kusekera kwabwino m' kuona kwako.
Zintu zonse zinaperekedwa kwa ine ndi Atatu wanga; 22
ndimo palibe muntu adziwa iemwe Mwana ali, koma Atate;
ndi iemwe Atate ali, koma Mwana, ndi ie kwa emwe Mwana
afuna ku sonyeza *ie.* Ndimo kutembenuka kwa akupun- 23
zira, nanena kutseri, Odala *ali* maso omwe aona zintu zomwe
muona: kuti dinena ndi inu, kuti ambiri aprofeti ndi 24
mafumu otshuka anafuna ku ona zintu zomwe muona,
ndimo sanaziona; ndi ku mva zintu zomwe mumva, ndimo
sanazimva.

Ndimo ona, nkoswe modzi naima nayesa ie, kuti, Mpun- 25
zitsi, didzatshita tshiani ku loa m' moyo wosamariza?
Ndimo nanena nai', Tshiani tshilembedwa m' mau? bwanje 26
uwerenga? Ndimo kuiang'ka nati, Udzakonda Mwini 27

Mulungu wako ndi ntima wako wonse, ndimo ndi nzimu
wako wonse, ndimo ndi mpamvu yako yonse, ndimo ndi
nzeru zako zonse; ndi woiandikila wako monga iwe eka.
28 Ndimo nanena nai', Waiang'ka bwino: tshita tshimene,
29 ndimo udzakala ndi moyo. Koma ie, kufuna ku dzide-
ketsa, nanena ndi Yesu, Ndimo ndani ali woiandikila
30 wanga? Yesu naiang'ka nati, Muntu modzi analikutsika
ku Yerusalem ku Yeriko; ndimo nagwa mwa olanda, omwe
nabvula ie nsaru zatshi nammenya, namuka, kusia ie
31 nafuna ku fa. Ndimo nangotsika ndzukuru modzi pa njira
imene: ndimo ntawi naona ie, nalambalala pa kundu lina.
32 Ndimo tshointsho onso Mlevi, ntawi anafika pa malo, ndimo
33 naona ie, nalambalala pa kundu lina. Koma Msamariya
modzi, monga naenda ulendo, nadza pomwe anali; ndimo
34 ntawi namona, anakala ndi tshisoni, nadza kwa ie, namanga
mabala atshi, kutsanula mafuta ndi vinyo; ndimo naika ie
pa nyama yatshi, namtenga ku bwalo, nayang'anira ie.
35 Ndimo mawa naturutsa madenariyon awiri, napatsa awo ku
mwini wa nyumba, nanena, Sungira ie; ndi tshomwe upatsa
36 tshopambana, ine, ntawi didza anso, didzalipira iwe. Uti
wa awa atatu, uganiza, anadzisonya woiandikila kwa ie
37 emwe anagwa mwa olanda? Ndimo nati, Iemwe nasonyeza
nsisi pa ie. Ndimo Yesu nanena nai', Muka, nutshita
modzimodzi.
38 Ndimo monga napita, naloa m' mudzi umodzi: ndimo
nkazi modzi atshedwa Marta nalandira ie m' nyumba yatshi.
39 Ndimo anali ndi mpwatshi atshedwa Mariya, iemwe enso
40 nakala pa mapazi a Mwini, namva mau atshi. Koma Marta
analemedwa ndi kuimirira kwambiri; ndimo nadza kwa ie,
nati, Mwini, kodi usasamala kuti mpwanga anandisiira ku
41 imirira ndeka? ndimo uza ie kuti atangate ine. Koma
Mwini naiang'ka nanena nai', Marta, Marta, uyang'anira
42 ndi kuganizaganiza ndi zintu zambiri: koma tshintu
tshimodzi tshifunidwa: kuti Mariya wasang'ka tshabwino
tshimene, tshomwe tshosadzatshotsedwa kwa ie.
11 Ndimo kunali, monga analikupempera m' malo amodzi,
kuti ntawi naleka, modzi wa akupunzira atshi nanena nai',
Mwini, punzitsa ife ku pempera, inde monga Yohane enso
2 napunzitsa akupunzira atshi. Ndimo nanena nao, Ntawi
mupempera, nenani, Atate, Liyeretsedwe dzina lako. Dziko
3 lako lidze. Patsa ife siku ndi siku kudia kwa siku.
4 Ndimo kululukira ife zakwaipa zatu; kuti ife toka anso

tikululukira onse omwe ali ndi mangawa ndi ife. Ndimo
usatenga ife m' tshinyengo.

Ndimo nanena nao, Ndani wa inu adzapotshera mbali, 5
ndimo adzang'ka kwa ie pakati pa usiku, nadzanena nai',
Mbali, bwereka ine mikate itatu; kuti mbali wanga wadza 6
kwa ine kwa ulendo, ndimo diribe kantu ku ika patsogolo
pa ie; ndimo ie kwa umo adzaiang'ka nati, Usandilongoloza: 7
tshitseko tshitsekedwa tsopano, ndimo ana anga ali ndi ine
m' kama; sindidziwa ku uka ndi ku patsa iwe? Dinena 8
ndi inu, Ngati wosadzauka ku patsa ie, tshifuka kuti ali
mbali watshi, kosuntira tshifuka tsha kuumirira kwatshi
adzauka nadzampatsa monga yambiri monga aifuna. Ndi- 9
mo dinena ndi inu, Funsani, ndimo tshidzapatsidwa kwa
inu; sakani, ndimo mudzapeza; gogodani, ndimo tshi-
dzatsegulidwa kwa inu. Kuti onse omwe afunsa alandira; 10
ndi emwe asaka apeza; ndi kwa emwe agogoda tshidza-
tsegulidwa. Ndimo wa emwe wa inu emwe ali atate mwana 11
watshi adzafunsa nkate, kodi adzampatsa mwala? kapena
nsomba, kodi ie kwa nsomba adzampatsa njoka? Kapena 12
*ngati* adzafunsa dzira, kodi adzampatsa tshinkanira? Ndimo 13
ngati inu, muli oipa, mudziwa bwanje ku patsa zolere
zabwino kwa ana anu, bwanje kopambana Atatu *anu*
amwamba adzapatsa Nzimu Woyera kwa awo omwe
amfunsa?

Ndimo analikuturutsa demon *emwe anali* wosalankula. 14
Ndimo kunali, ntawi demon naturuka, wosalankula nala-
nkula; ndi antu ambiri nazizwa. Koma ena a awo nati, 15
Ndi Belzebule fumu ya ademon aturutsa ademon. Ndimo 16
ena, ku*m*yesa, afunsa ie tshizindikilo kwa kumwamba.
Koma ie, kudziwa matintu ao, nanena nao, Dziko lonse 17
lagawidwa pa loka litengedwa ku bwinja; ndi nyumba
*inagawidwa* pa nyumba igwa. Ndimo ngati Satana anso 18
agawidwa pa eka, bwanje dziko latshi lidzaima? tshifuka
munena kuti diturutsa ademon ndi Belzebule. Ndimo ngati 19
ine ndi Belzebule diturutsa ademon, ana anu aturutsa ndi
ani? ndimo awa adzakala oweruza anu. Koma ngati ine 20
ndi tshala tsha Mulungu diturutsa ademon pomwe dziko la
Mulungu linafika pa inu. Ntawi *muntu* wolimba anali ndi 21
ntungo asunga kuka kwatshi, zintu zatshi ziri ndi ntendere:
koma ntawi wolimba wopambana ie adzafika pa ie, nadza- 22
tsitsa ie atshotsa kwa ie tshamuna tshatshi tshonse mwa
tshomwe namvana, nagawa zintu zatshi za nkondo. Iemwe 23

wosali ndi ine ali pa ine; ndi iemwe wosakung'ka ndi ine
24 ataia. Nzimu wosatsuka ntawi unaturuka kwa muntu,
uenda pandule malo opanda madzi, kusaka kupuma; ndimo
usapeza, uti, Didzabwera ku nyumba yanga yomwe dinatu-
25 ruka. Ndimo ntawi unafika, uipeza yosesedwa ndi
26 yokonzedwa. Pomwe upita, nutenga *ku iwo* mizimu isanu
ndi iwiri ina yoipa yopambana ndi iwo; ndimo iloa nikala
umo: ndimo makalidwe akutungo a muntu amene ali oipa
opambana apatsogolo.
27 Ndimo kunali, monga nanena zintu zimenezi, nkazi modzi
wa antu ambiri natukula liu latshi, nanena nai', Tshodala
tshiri tshibaliro tshomwe tshabala iwe, ndi maere omwe
28 unamwa. Koma nanena, Inde opambana, odala ali awo
omwe amva mau a Mulungu, naasunga.
29 Ndimo ntawi antu ambiri analikusong'kana kwa ie, naamba
ku nena, Fuko limene liri fuko loipa: lisaka tshizindikilo;
ndimo palibe tshizindikilo tshidzapatsidwa kwa ilo koma
30 tshizindikilo tsha Yona. Kuti inde monga Yona anali
tshizindikilo ku Aninive, tshointsho onso Mwana wa muntu
31 adzakala ku fuko limene. Fumu yeikazi yotshuka ya
kumwela idzauka m' kuweruza ndi antu a fuko limene,
ndimo idzasutsa awo: kuti inadzera kwa malo akutali ku
mva nzeru za Solomon; ndimo ona, wang'kuru ndi Solomon
32 ali pano. Amuna a Ninive adzauka mwa kuweruza ndi
fuko limene, ndimo adzalisutsa: kuti natembenuka pa kuuza
kwa Yona; ndimo ona, wang'kuru ndi Yona ali pano.
33 Palibe muntu, ntawi anaatsa muni, auika m' malo
akutseri, kapena pansi pa ntanga, koma pa tshogwirira, kuti
34 awo omwe aloa angoona kuunika. Muni wa tupi lako uli
diso lako: ntawi diso lako liri limodzi, tupi lako lonse
enso liri lodzaza ndi kuunika; koma ntawi liri loipa, tupi
35 lako onso lidzaza ndi ndima. Ndimo yang'anirani kuti
36 kuunika komwe kuli mwa iwe sikuli ndima. Ndimo ngati
tupi lako lonse liri lodzaza ndi kuunika, kuli ndi palibe
malo a ndima, lonse lidzadzaza ndi kuunika, monga ntawi
muni ndi kuwala kwabwino kwatshi ukupatsa kuunika.
37 Ndimo monga nanena, Mfarisi afunsa ie ku dia nai':
38 ndimo naloa, nakala pansi pa kudia. Ndimo ntawi
Mfarisi naona, nazizwa kuti pakuamba sanasamba patsogolo
39 kudia. Ndimo Mwini nanena nai', Tsopano Afarisi inu
mutsukitsa kunja kwa tshiko ndi kwa mbale; koma pakati
40 panu padzaza ndi kubera ndi mpulupulu. Mwapusa inu,

kodi iemwe anapanga tshomwe tshiri kunja napanga
tshomwe tshiri mbwalo onso? Koma patsani kwa zolere 41
zintu zimenezo zomwe ziri umo; ndimo ona, zintu zonse
ziri zotsuka kwa inu.

Koma tshaipa kwa inu Afarisi! kuti mupatsa mpambu ya 42
minte ndi rue ndi zitsamba zonse, ndimo muleka kuweruza
ndi kukonda za Mulungu: koma zimenezi mukanatshita,
ndimo sikuleka kena kosatshitidwa. Tshaipa kwa inu 43
Afarisi! kuti mukonda mipando yopambana m' masinagoge,
ndi mautso m' mabwalo a maronda. Tshaipa kwa inu! 44
kuti muli monga mianda yomwe yosasonyeza, ndimo antu
omwe apita pamwamba pa *iyo* osadziwa iyo.

Ndimo modzi wa ankoswe kuiang'ka anena nai', Mpunzitsi, 45
m' kunena tshointsho udzudzula ife enso. Ndimo nati, 46
Tshaipa kwa inu unso ankoswe! kuti musenza antu ndi
akatundu olemera ku nyamulidwa, ndi inu noka musatosa
akatundu ndi tshimodzi tsha dzala dzako. Tshaipa kwa 47
inu! kuti mumanga mianda ya aprofeti, ndi atatu anu
anaapa. Tshointsho muli omariza ndi mubvomereza ntshito 48
za atatu anu: kuti anapa awa, ndimo mumanga *mianda yao.*
Ndimo onso inanena nzeru ya Mulungu, Didzatumiza ku 49
awo aprofeti ndi apostile; ndi *ena* a awa adzapa nadzazunza;
kuti mwazi wa aprofeti onse, womwe waturutsidwa kwa 50
kuzika kwa dziko, ungofunidwa ndi fuko limene; kwa 51
mwazi wa Habeli ku mwazi wa Zekariya, emwe namwazidwa
pakati pa katshisi ndi nyumba: inde, dinena ndi inu,
udzafunidwa kwa fuko limene. Tshaipa kwa inu ankoswe! 52
kuti munatshotsa mfungulo ya kudziwa: simunaloa inu noka,
ndi awa omwe analikuloa munatshedwetsa.

Ndimo ntawi naturuka umo, akulembera ndi Afarisi 53
naamba ku*m*kakamiza kwambiri, ndi kumputa ku nena ndi
zintu zambiri; kubisalira ie, ku gwira kantu m' nkamwa 54
mwatshi.

12 Ntawi yomwe, ntawi antu ambiri osawereng'jeka anaso-
ng'kanidwa, monga ambiri kuti anaponda modzi pa wina,
naamba ku nena ndi akupunzira atshi, patsogolo pa onse,
Tshenjerani inu ndi fumba ya Afarisi, yomwe iri tshinyengo.
Koma palibe kantu kovundukilidwa, komwe kosadzasonye- 2
zedwa: ndi kobisidwa, komwe kosadzadziwidwa. Ndimo 3
tshomwe mwanena mudima tshidzamvedwa m' kuunika;
ndi tshomwe mwanena m' kutu m' dzipinda tshidzauzidwa pa
matshindu. Ndimo dinena ndi inu abali anga, Musaopa 4

awo omwe apa tupi, ndi pambuiu kumene osapotshera kantu
5 komwe adziwa ku tshita. Koma didzatshenjeza inu emwe
mudzaopa: Opani ie, emwe pambuiu anapa ali ndi mpamvu
6 ku ponya m' geena; inde, dinena ndi inu, Opani ie. Kodi
sikuli mpiningo zisanu zigulitsidwa kwa mafardin awiri?
ndimo palibe imodzi ya izo iwalidwa patsogolo pa Mulungu.
7 Koma inde matsisi a mutu wanu onse awerengedwa.
8 Musaopa: muli opambana mpiningo zambiri. Ndimo dinena
ndi inu, Emwe adzabvomera ine patsogolo pa antu, ie
Mwana wa muntu unso adzabvomera patsogolo pa anjelo a
9 Mulungu: koma iemwe akana ine patsogolo pa antu adza-
10 kanidwa patsogolo pa anjelo a Mulungu. Ndimo iemwe
adzanena liu pa Mwana wa muntu, kudzakululukidwa ie:
koma kwa iemwe atukwana pa Nzimu Woyera kosadzakulu-
11 lukidwa. Ndimo ntawi atenga inu kwa masinagoge, ndi
kwa oweruza, ndi ampamvu, musaganizaganiza bwanje
kapena tshintu tshiti mudzaiang'ka, kapena tshomwe
12 mudzanena: kuti Nzimu Woyera udzapunzitsa inu mwa
ora limeneli tshomwe mukananena.
13 Ndimo modzi wa antu ambiri nanena nai', Mpunzitsi, uza
14 njiranga ku gawa zoloa ndi ine. Koma nanena nai',
Mamuna, ndani wapanga ine woweruza kapena wogawa pa
15 inu? Ndimo nanena nao, Yang'anirani, ndi mudzisungire
kwa kusirira konse: kuti moyo wa muntu wosakala ndi
16 zambiri za zintu zomwe azipotshera. Ndimo nanena nao
fanizo, kuti, Ntaka ya muntu modzi wolemera inabala
17 zambiri: ndimo naganiza mwa ie eka, kuti, Didzatshita
tshiani, tshifuka sindipotshera malo pomwe ku ika dzobala
18 dzanga? Ndimo nati, Tshimene didzatshita: didzagwetsa
nkokwe zanga, didzamanga zazikuru; ndimo apo didzaika
19 dzintu dzanga dzonse ndi zintu zanga. Ndimo didzanena
ndi nzimu wanga, Nzimu, uli ndi zintu zambiri zaikidwa
kwa dzaka dzambiri; tenga kupuma kwako, udie, umwe,
20 usekere. Koma Mulungu nanena nai', Wapusa iwe, siku
limene nzimu wako udzafunidwa kwa iwe: ndimo zintu
21 zomwe unazikonzetsa, zidzakala za ani? Tshointshi ali
iemwe aika kulemera kwa ie eka, ndimo wosali wolemera
kwa Mulungu.
22 Ndimo nanena ndi akupunzira atshi, Ndimo dinena ndi
inu, Musaganizaganiza kwa moyo *wanu*, tshomwe mudzadia;
kapena kosuntira kwa tupi lanu, tshomwe mudzabvala.
23 Kuti moyo uli wopambana kudia, ndi tupi lopambana nsaru.

Ganizani ndi makungubwi, kuti kapena osafesa, kapena 24
osatema; omwe osapotshera nyumba ya dzintu kapena
nkokwe; ndimo Mulungu aeta awa: ntengo wapatali
bwanje muli opambana zimbalame! Ndimo ndani wa inu 25
ndi kuganizaganiza adziwa ku ong'khetsa nkono ku nsing'ku
watshi? Ndimo ngati musali ndi mpamvu ku tshita inde 26
tshimene tshomwe tshiri tshatshing'ono tshopambana,
muganizaganiza bwanje ndi zotsala? Ganiza ndi dzikombo- 27
kombo, bwanje dzimera: dzosatshita kolimba, kapena
dzosapota; koma dinena ndi inu, Inde Solomon m' kupa-
mbana kwatshi konse sanabvalira kofana ndi tshimodzi tsha
idzo. Koma ngati Mulungu tshointsho abveka maudzu m' 28
munda, omwe lero akala, ndi mawa aponyedwa m' stoko;
bwanje kopambana *adzabveka* inu, O inu a mvanu ung'ono?
Ndimo musafuna tshomwe mudzadia, ndi tshomwe mudza- 29
mwa, kapena musakala ndi ntima woganizaganiza. Kuti 30
zintu zonse zimenezi mitundu ya dziko ifuna: koma Atatu
anu adziwa kuti muli ndi kufunidwa ndi zintu zimenezi.
Koma funani dziko latshi, ndimo zintu zimenezi zidzao- 31
ng'khetsedwa kwa inu. Musaopa, kagulu kang'ono; kuti 32
kuli kufuna kwabwino kwa Atatu anu ku patsa inu dziko.
Gulitsani zomwe muli nazo, ndimo patsani zolere; konzetsani 33
inu noka timatumba tomwe tosakala takali, kulemera m'
miamba komwe kosaleka, komwe kulibe woba woyandika,
kapena tshikululu tshibvunditsa. Kuti pomwe kulemera 34
kwanu kuli, pomwe ntima wanu udzali inso.

Mtshuuno mwanu mudzakale momangidwa, ndi miuni 35
yanu iake; ndimo kalani inu noka ofana ndi antu kuyang'- 36
anira mwini wao, ntawi adzabwera kwa kudia kwa kukwa-
titsa; kuti, ntawi afika nagogoda, angotsegula kwa ie
tsopano lino. Odala ali akapolo amene, omwe mwini ntawi 37
afika adzapeza kudikira: dinena ndi inu nditu, kuti adza-
mangitsa ie eka, napanga awa ku kala pansi pa kudia,
ndimo adzafika nadzaimirira awo. Ndimo ngati adzafika 38
m' kudikira kwatshiwiri, ndimo ngati m' kwatshitatu, napeza
*awo* tshointsho, odala ali amenewo. Koma dziwani tshime- 39
netshi, kuti ngati mwini wa nyumba anadziwa mwa ora liti
woba analikufika, akanadikira, ndimo sanasia nyumba yatshi
ku boledwa. Kalani inso akuta: kuti mwa ora lomwe 40
musaganiza Mwana wa muntu afika.

Ndimo Petros nanena, Mwini, kodi unena fanizo limene 41
kwa ife, kapena inde kwa onse? Ndimo Mwini nati, 42

Ndimo ndani ali ndindo wamvanu ndi wanzeru, emwe mwini
watshi adzaika pa banja latshi, ku patsa awo poso lao pa
43 ntawi yabwino. Wodala ali kapolo amene, emwe mwini
44 watshi ntawi afika adzapeza kutshita tshointsho. Dinena
ndi inu koona, kuti adzamwika pa zonse zomwe ali nazo.
45 Koma ngati kapolo amene adzanena mutima mwatshi,
Mwini wanga atshedwetsa kufika kwatshi; ndimo adzaamba
ku menya abandazi ndi abandazi akazi, ndimo ku dia ndi
46 ku mwa, ndi ku ledzedwa; mwini wa kapolo amene adzafika
m' siku ntawi wosayang'anira, ndi mwa ora ntawi wosadziwa,
ndimo adzamdula pakati, ndimo adzaika malo atshi ndi
47 osamvana. Ndimo kapolo amene, emwe nadziwa kufuna
kwa mwini watshi, ndimo sanakonzetsa, kapena sanatshita
kofana ndi kufuna kwatshi, adzamenyedwa ndi *mikakato*
48 yambiri; koma emwe sanadziwa, ndimo natshita zintu
zoenera za mikakato, adzamenyedwa ndi *mikakato* yowe-
reng'jeka. Ndimo kwa emwe zambiri zinapatsidwa, ndi ie
zambiri zidzafunidwa: ndimo kwa emwe apatsa zambiri,
ndi ie adzafunsa zopambana.
49 Dinafika ku ponya moto pa dziko; ndimo difuna tshiani,
50 ngati tsopano waatsidwa? Koma diri ndi mbapatisma ku
bapatizidwa na*lo;* ndimo bwanje diri ndi kufuna kwa ntawi
51 lidzatedwa! Kodi muganiza kuti dinafika ku patsa ntendere
m' dziko? Dikuuzani, Iai; koma kopambana kugawa:
52 kuti kwa ntawi imene kudzali asanu m' nyumba imodzi
53 agawidwa, atatu pa awiri, ndi awiri pa atatu. Adzagawi-
dwa, atate pa mwana wamamuna, ndimo mwana wamamuna
pa atate; amai pa mwana wankazi, ndi mwana wankazi pa
amai atshi; mpongozi pa mpongozi watshi, ndi mpongozi
pa mpongozi watshi.
54 Ndimo nanena anso kwa antu ambiri, Ntawi muona
ntambo kuturuka ku zambwe, tsopano lino munena, Kudza
55 mvula; ndimo kuli tshointsho. Ndimo ntawi mwela uomba,
56 munena, kudzali kutenta kwambiri; ndimo kuli. Atshi-
nyengo inu, mudziwa bwanje ku dziwitsa nkope ya dziko
ndi ya mlengalenga; koma kuli bwanje kuti musadziwa ku
57 dziwitsa ntawi imene? Ndimo bwanje inde ndi inu noka
58 musaweruza tshomwe tshiri tshabwino? kuti monga uliku-
enda ndi liwongo lako patsogolo pa woweruza, pa njira
yang'anira bwino kuti ungopulumuka kwa ie; kani kapena
atsogoza iwe ku woweruza, ndimo woweruza adzapereka
iwe kwa kazembe, ndi kazembe adzaponya iwe m' nyumba

ya ndima. Dikuuza, Usadzaturuka umo nditu kwa ntawi 59
walipira kamite kakutungo.

Ndimo kunali pa ntawi imene ena omwe nauza ie ndi 13
Agalileya, mwazi wa omwe Pilato anasang'kaniza ndi nsembe
zao. Ndimo naiang'ka nanena nao, Kodi muganiza kuti 2
Agalileya amene anali ampulupulu opambana Agalileya
onse, tshifuka anamva zintu zimenezi? Dikuuzani, Iai: 3
koma, kani mutembenuza mitima, mudzamwazika nonse
tshointsho. Kapena adya kumi ndi asanu ndi atatu, pa 4
omwe nsanja m' Silowa inagwa, ndimo inapa awo, kodi
muganiza kuti anali amangawa opambana antu onse omwe
akala m' Yerusalem? Dikuuzani, Iai: koma, kani mute- 5
mbenuza mitima, mudzamwazika nonse enso.

Ndimo nanena fanizo limene; Muntu modzi anali ndi 6
ntengo wa nkhuyu unaokedwa m' munda wa mvina watshi;
ndimo nadza kufuna dzobala pa iwo, napeza palibe. Ndimo 7
nanena ndi wotshita m' munda, Ona, dzaka dzitatu dzime-
nedzi didza kusaka dzobala pa ntengo wa nkhuyu umene,
ndimo dipeza palibe: dula iwo; bwanje iwo onso usakaza
ntaka? Ndimo ie kuiang'ka anena nai', Mwini, reka iwo 8
tshaka tshimenetshi inso, kwa ntawi didzakumba kozungu-
lira iwo, nditukusa iwo: ndimo ngati kwa ntawi yatsopano 9
ubala dzobala, *bwino;* koma ngati iai, udzadula iwo.

Ndimo analikupunzitsa m' limodzi la masinagoge pa dzua 10
la sabata. Ndimo ona, nkazi emwe anali ndi nzimu wa 11
kufoka dzaka kumi ndi dzisanu ndi dzitatu; ndimo nawera-
midwa, ndimo sanadziwa ku ong'goka konse eka. Ndimo 12
ntawi Yesu namona, namwitana, nanena nai', Nkazi, umasu-
lidwa kwa kufoka kwako. Ndimo naika manja atshi pa ie: 13
ndimo tsopano lino nalungamitswa, napambanitsa Mulungu.
Ndimo woweruza wa sinagoge, kusuntidwa ndi kukwia, 14
tshifuka kuti Yesu anatshiritsa pa sabata, naiang'ka nanena
ndi antu ambiri, Kunali masiku asanu ndi limodzi mwa
omwe antu akanagwira ntshito: ndimo mwa iwo idzani ndi
mutshiritsidwa, ndimo si pa dzua la sabata. Koma Mwini 15
naiang'ka ie, nati, Atshinyengo inu, kodi inu nonse pa
sabata mumasula ng'ombe yanu kapena buru wanu kwa
malo ao, ndi mutsogoza izo ku kumwa madzi? Ndimo 16
kodi nkazi amene, ali mwana wankazi wa Abraham, iemwe
Satana anamanga, ona, dzaka kumi ndi dzisanu ndi dzitatu,
akanadza masulidwa kwa tshomangira tshimene pa dzua la
sabata? Ndimo monga ananena zintu zimenezi, maliwongo 17

atshi onse anapatsidwa manyazi: ndi antu onse nasekera
kwa zintu zonse zopambana zomwe zinatshitidwa ndi ie.
18 Ndimo nati, Dziko la Mulungu liri lofana ndi tshiani?
19 ndimo kwa tshiani didzafaniza ilo? Liri lofana ndi mpetshe
ya mostade, yomwe muntu natenga, naponya m' munda
mwatshi: ndimo inamera, ndimo inakala ntengo; ndi
20 mbalame za mlengalenga zinakala m' matsatsa a iwo. Ndimo
nanena anso, Didzafaniza dziko la Mulungu ndi tshiani?
21 Liri lofana ndi fumba, yomwe nkazi natenga nabisa m'
miezo itatu ya ufa, kwa ntawi wonse watupitsidwa.
22 Ndimo napita m' mizinda ndi m' midzi, kupunzitsa, ndi
23 kuenda ku Yerusalem. Ndimo modzi nanena nai', Mwini,
kodi ali owereng'jeka omwe apulumutsidwa? Ndimo
24 nanena nao, Yesani ku loa pa tshitseko tshopapatiza: kuti
ambiri, dinena ndi inu, adzafuna ku loa, ndimo sadzadziwa.
25 Ntawi Mwini wa nyumba wauka, ndimo watseka tshitseko,
ndimo muamba ku ima kunja, ndi ku gogoda pa tshitseko,
kuti, Mwini, tsegula kwa ife; ndimo adzaiang'ka nadzanena
26 ndi inu, Sindidziwa inu komwe mudzera; pomwe mudza-
amba ku nena, Tinadia ndimo tinamwa patsogolo pa iwe,
27 ndimo unapunzitsa m' makwalala atu; ndimo adzanena,
Dikuuzani, sindidziwa inu komwe mudzera; tshokani kwa
28 ine, inu nonse otshita a mpulupulu. Pomwe kudzali
kulira, ndi kukukuta mano, ntawi mudzaona Abraham,
ndi Yisake, ndi Yakobi, ndi aprofeti onse, m' dziko
29 la Mulungu, ndi inu noka munaturutsidwa kunja. Ndimo
adzadzera ku bvuma ndi ku zambwe, ndi ku mpoto ndi
ku mwela, ndimo adzakala pansi m' dziko la Mulungu.
30 Ndimo ona, kuli akutungo omwe adzali oiamba, ndimo kuli
oiamba omwe adzali akutungo.
31 M' ora lomwe kunadza ena a Afarisi, kunena ndi ie,
Turuka iwe, tshoka pano: kuti Herode afuna ku pa iwe.
32 Ndimo nanena nao, Mukani, uzani nkhandwe amene, Ona,
diturutsa ademon ndimo ditshita matshiritso lero ndi mawa,
33 ndimo nkutsha ditedwa. Koma dikanaenda lero ndi
mawa ndi nkutsha: kuti kusadzali kuti mprofeti amwa-
34 zika kunja kwa Yerusalem. O Yerusalem, Yerusalem,
womwe upa aprofeti, nuponya miala awo omwe atumidwa
kwa iwo! bwanje zambiri dafuna ku song'kanitsa ana ako,
inde monga nkuku yatadzi *isong'kanitsa* anapie atshi pansi
35 pa mapiko atshi, ndimo simunafuna! Ona nyumba yako
isiidwa *dzinja* kwa inu: ndimo dinena ndi inu, Simudzaona

ine, kwa ntawi mudzanena, Wodala *ali* iemwe adza m' dzina
la Mwini.

Ndimo kunali, ntawi naloa m' nyumba ya modzi wa 14
akuru a Afarisi pa sabata ku dia nkate, kuti analikudikira
ie. Ndimo ona, kunali muntu modzi patsogolo pa ie emwe 2
anali ndi tsempo. Ndimo Yesu kuiang'ka nanena ndi 3
ankoswe ndi Afarisi, kuti, Kodi tshiri tshamau ku tshiritsa
pa sabata, kapena iai? Koma nakala tshete. Ndimo 4
natenga ie, namtshiritsa, namleka ku ng'ka. Ndimo nanena 5
nao, Ndani wa inu adzakala ndi buru kapena ng'ombe
zinagwa m' tshitsime, ndimo wosafuna tsopano lino ku koka
izo pa dzua la sabata? Ndimo sanadziwa ku yang'ka anso 6
ndi zintu zimenezi.

Ndimo nanena fanizo kwa awo omwe anaitanidwa, ntawi 7
naona bwanje nasang'ka malo akuru; kunena nao, Ntawi 8
uitanidwa ndi muntu modzi kwa kudia kwa kukwatitsa,
usakala pansi m' malo opambana; kani kapena muntu ndi
ulemu wopambana ndi iwe aitanidwa ndi ie, ndimo iemwe 9
anaitana iwe ndi ie adzafika nadzanena ndi iwe, Patsa muntu
amene malo; ndimo pomwe udzaamba ndi manyazi ku
tenga malo apansi opambana. Koma ntawi uitanidwa, 10
enda nukala m' malo apansi opambana; kuti ntawi emwe
wakuitana adza, angonena ndi iwe, Mbali, pita pamwamba:
pomwe udzakala ndi kupambana patsogolo pa onse omwe
akala pa kudia ndi iwe. Kuti iemwe adzikulitsa adzatshe- 11
petsedwa; ndi iemwe adzifatsitsa adzakulitsidwa.

Ndimo nanena anso ndi ie emwe anaitana ie, Ntawi 12
upanga kudia kwa nsana kapena ngonero, usaitana ma-
bwenzi ako, kapena abali ako, kapena fuko lako, kapena
oiandikila olemera; kani kapena awo onso akuitana iwe
enso, ndimo kulipira kupangidwa ndi iwe. Koma ntawi 13
upanga kudia, itana osauka, opunduka mikono, opunduka
miendo, akungu: ndimo udzadalitsidwa; tshifuka siali ndi 14
*kantu* ku lipira iwe: kuti udzalipidwa pa kuukirira kwa
odeka.

Ndimo ntawi modzi wa awa omwe nakala pa kudia nai' 15
anamva zintu zimenezi, nanena nai', Wodala ali emwe
adzadia nkate m' dziko la Mulungu. Koma nanena nai', 16
Muntu modzi napanga ngonero wambiri; ndimo naitana
ambiri: ndimo natuma kapolo watshi pa ntawi ya ngonero 17
ku nena nao omwe anaitanidwa, Idzani; kuti zintu *zonse*
tsopano zata. Ndimo awa onse ndi *ntima* umodzi naamba 18

ku panga pambanuzo. Woiamba nanena nai', Dagula
munda, ndimo dikanaenda kuuona: dipempa iwe ku
19 pambanuza ine. Ndimo wina nati, Dagula zikondo zisanu
za ng'ombe, ndimo ding'ka ku yesa izo: dipempa iwe ku
20 pambanuza ine. Ndimo wina nati, Dakwata nkazi, ndimo
21 tshointsho sindidziwa ku dza. Ndimo kapolo nadza, nauza
mwini watshi zintu zimenezi. Pomwe mwini wa nyumba
ali ndi kukwia nanena ndi kapolo watshi, Enda nsanga mwa
makwalala ndi njira za mzinda, nutenga muno osauka ndi
opunduka mikono ndi akungu ndi opunduka miendo.
22 Ndimo kapolo nati, Mwini, tshomwe unauza tshitshitidwa,
23 ndimo kosuntira alipo malo. Ndimo mwini nanena ndi
kapolo, Muka m' zinjira ndi m' matshinga, nufulumiza *awo*
24 ku loa, kuti nyumba yanga ingodzazidwa. Kuti dinena
ndi inu, kuti palibe modzi wa antu amenewo omwe anait-
anidwa adzalawa ngonero wanga.
25 Ndimo anang'ka nai' antu ambiri: ndimo natembenuka,
26 nanena nao, Ngati muntu modzi adza kwa ine, ndi wosa-
kwiira atatu atshi, ndi amai *atshi*, ndi nkazi, ndi ana, ndi
abali, ndi alongo *atshi*, inde, ndi moyo watshi inso, wosa-
27 dziwa ku kala wakupunzira wanga. Iemwe wosanyamula
nkhwitshi yatshi, nanditsata, wosadziwa ku kala wakupu-
28 nzira wanga. Kuti ndani wa inu, kufuna ku manga nsanja,
wosakala pansi patsogolo ku werenga ntengo watshi, ngati
29 anali ndi *zambiri* ku ta iyo? Kani kapena, ntawi waika
kuzika, ndimo wosali ndi mpamvu ku ta, onse omwe aona
30 aamba ku nyoza ie, kuti, Muntu amene naamba ku manga,
31 ndimo wosali ndi mpamvu ku ta. Kapena fumu yotshuka
ndani, monga ienda ku panga nkondo pa fumu yotshuka
ina, kodi yosakala pansi patsogolo niganiza ngati inali ndi
mpamvu ndi mazousan kumi ku komana ndi iyo yomwe
32 idza pa iyo ndi mazousan makumi awiri? Kapena kani,
ntawi ina tsopano iri kosuntira kutali, itumiza mitenga,
33 nifunsa mau a ntendere. Ndimo tshointsho ie wa inu emwe
wosasia zonse zomwe ali nazo, wosadziwa ku kala waku-
34 punzira wanga. Ndimo ntshere uli wabwino: koma inde
ngati ntshere unataiika nyongo yatshi, ndi tshiani udza-
35 kometsedwa? Suli wabwino kapena kwa ntaka kapena
kwa dzara: *antu* aturutsa iwo. Iemwe ali makutu ku mva,
amve.

15 Ndimo akulandira tsong'ko onse ndi ampulupulu ana-
2 likuandika ie kuti amve ie. Ndimo Afarisi ndi akulembera

nandandaula, kuti, Muntu amene alandira ampulupulu,
nadia nao.
Ndimo nanena nao fanizo limene, kuti, Muntu uti wa 3,4
inu, ali ndi nkosa makumi okaoka kumi, ngati anataia
imodzi ya izo, wosasia makumi asanu ndi anai, ndi zisanu
ndi zinai m' tshipululu, natsata yomwe yataiika, kwa ntawi
naipeza? Ndimo ntawi naipeza, aiika pa mapuzi atshi, 5
kusekera. Ndimo ntawi afika kwatshi, asong'kanitsa abali 6
atshi ndi oiandikila atshi, kunena nao, Sekerani ndi ine,
kuti dapeza nkosa yanga yomwe inataiika. Dinena ndi 7
inu, kuti inde tshointsho tshidzakala tshimwemwe m'
mwamba pa wampulupulu modzi emwe atembenuza ntima,
tshopambana pa antu odeka makumi asanu ndi anai, ndi
asanu ndi anai, omwe osafuna kutembenuza ntima.
Kapena nkazi uti ali ndi madrakim kumi, ngati ataia 8
limodzi, wosaatsa nyali, nasesa nyumba, nafuna kwatshangu
kwa ntawi apeza ilo? Ndimo ntawi wapeza ilo, asong'- 9
kanitsa abali atshi ndi oiandikila, kuti, Sekerani ndi ine,
kuti dapeza didrakim lomwe dinataia. Inde tshointsho, 10
dinena ndi inu, tshiri tshimwemwe patsogolo pa anjelo a
Mulungu pa wampulupulu modzi emwe atembenuza ntima.
Ndimo nati, Muntu modzi anali ndi ana awiri: ndimo 11.12
wang'ono wa awa nanena ndi atatu atshi, Atate, patsa ine
pande la zintu *zako* lomwe lirinkudza kwa ine. Ndimo
nagawira awo moyo watshi. Ndimo si masiku ambiri 13
pambuiu mwana wang'ono nasong'ketsa zonse, natenga
ulendo watshi ku dziko lakutali; ndi pomwe namwaza zintu
zatshi koledzera. Ndimo ntawi anamwaza zonse, kudzakala 14
tshaola tshatshikuru m' dziko limene; ndimo naamba ku kala
ndi kusauka. Ndimo nang'ka nadzipatika ndi modzi wa 15
amuzinda a dziko limene; ndimo ie namtuma ku minda
yatshi ku eta nkhumba. Ndimo nafuna ku kutitswa ndi 16
madea omwe nkhumba zinadia: ndimo palibe muntu
napatsa kwa ie. Koma ntawi naganiza eka nati, Olipidwa 17
angati a atatu anga ali ndi mikate yokuta ndi ku leka,
ndimo dimwazika kuno ndi njala! Didzauka ndienda kwa 18
atatu anga, ndidzanena nai', Atate, dalapa pa kumwamba,
ndi m' kuona kwako: sindiri woenera anso ku tshedwa 19
mwana wako: panga ine monga modzi wa olipidwa ako.
Ndimo nauka, nadza ku atatu atshi. Koma ntawi anali 20
kosuntira kutali, atatu atshi namona, nakala ndi tshisoni,
natamanga, nagwa pa kosi latshi, namsomsona. Ndimo 21

mwana nanena nai', Atate, dalapa pa kumwamba, ndi m'
kuona kwako: sindiri woenera anso ku tshedwa mwana
22 wako. Koma atate nanena ndi akapolo atshi, Turutsani
nsanga mwinjiro wopambana, ndimo muike uo pa ie; ndimo
muike mpete pa dzanja latshi, ndi dzikwakwata pa mapazi
23 atshi: ndimo tengani mwana wa ng'ombe wonenepetsedwa,
24 mumpe, ndimo tidie, ntisekere; kuti ămene mwana wanga
anafa, ndimo ali ndi moyo onso; anataiika, ndimo apezedwa.
25 Ndimo anaamba ku sekera. Ndimo mwana watshi wa-
ng'kuru anali m' munda: ndimo monga anadza, naandika
26 nyumba, namva kuimba ndi kubvina. Ndimo naitana kwa
ie modzi wa akapolo, nafunsa zintu zimenezi zinangokala
27 bwanje. Ndimo nanena nai', Mpwako anafika; ndimo
atatu ako wapa mwana wa ng'ombe wonenepetsedwa,
28 tshifuka walandira ie wopulumuka ndi wolimba. Koma
nakwia, ndimo sanafuna ku loa: ndimo atatu atshi na-
29 turuka, napempa ie. Koma naiang'ka nanena ndi atatu
atshi, Ona, dzaka dzimene dzambiri diimirira iwe, ndimo
sindaswa ntawi ina mau ako: ndimo *kosuntira* usanapatsa
ine ntawi ina mwana wa gogo, kuti dinangosekera ndi abali
30 anga: koma ntawi amene mwana wako anadza, emwe wadia
moyo wako ndi akazi atshigololo, wapa kwa ie mwana wa
31 ng'ombe wonenepetsedwa. Ndimo nanena nai', Mwana, uli
ndi ine ntawi yonse, ndi zonse zomwe ziri za ine ziri zako.
32 Koma kunali bwino ku sekera ndi ku kondwera: kuti
amene mpwako anafa, ndimo ali ndi moyo *onso;* ndimo
nataiika, ndimo apezedwa.

16 Ndimo nanena anso ndi akupunzira, Kunali muntu
modzi wolemera, iemwe anali ndi ndindo; ndi emwe
anatshulidwa ndi ie kuti analikusakaza zintu zatshi.
2 Ndimo naitana ie, nanena nai', Tshimene tshiri tshiani
tshomwe dimva ndi iwe? tshula kuwerengera kwa udindo
3 wako; kuti usadziwa ku kala anso ndindo. Ndimo ndindo
nanena muntima watshi, Didzatshita tshiani, kuona kuti
mwini wanga atshotsa kwa ine udindo? Sindiri ndi
4 mpamvu ku lima; ku pempa diri ndi manyazi. Dili-
mbikira tshiani ku tshita, kuti, ntawi ditshotsedwa mwa
5 udindo, angolandira ine mwa nyumba zao. Ndimo kuitana
kwa ie amangawa onse a mwini watshi, nanena ndi woamba,
6 Ukong'gola bwanje ndi mwini wanga? Ndimo nati, Miyezo
makumi okaoka kumi ya mafuta. Ndimo nanena nai',
Tenga nkarata wako, nukala pansi nsanga nulemba makumi

asanu. Ndimo nanena ndi wina, Ndimo iwe ukong'gola 7
bwanje? Ndimo nati, Miyezo makumi okaoka kumi ya
trigu. Anena nai', Tenga nkarata wako, nulemba makumi
asanu ndi atatu. Ndimo mwini watshi nasimba ndindo 8
wosadeka tshifuka anatshita kotshenjera: kuti ana a
kugonera kumene ali kwa fuko lao otshenjera opambana
ana a kuunika. Ndimo dinena ndi inu, Pangani kwa inu 9
noka abali ndi kulemera za kusadeka; kuti, ntawi kudzale-
pera, angolandira inu mwa masasa osamariza. Iemwe ali 10
wamvanu m' komwe kali kakang'ono ali wamvanu unso m'
kwakukuru: ndimo iemwe ali wosadeka m' kakang'ono ali
wosadeka anso m' kwakukuru. Ndimo ngati musanakala 11
amvanu m' kulemera kwa kusadeka, ndani adzapatsa kwa
mvanu wanu *zolemera* zoona? Ndimo ngati musanakala 12
amvanu m' tshimene tshomwe tshiri tsha wina, ndani
adzapatsa inu, tshomwe tshiri tshanu? Palibe bandazi 13
adziwa ku imirira eni awiri: kuti kapena adzakwia ndi
modzi, nadzakonda wina; kapena kani adzakala ndi modzi,
nadzanyoza wina. Simudziwa ku imirira Mulungu ndi
kulemera.

Ndimo Afarisi, omwe anali okonda ndrama, anamva 14
zintu zonse zimenezi; ndimo naseka ie. Ndimo nanena nao, 15
Muli awo omwe mudzideketsa m' kuona kwa antu; koma
Mulungu adziwa mitima yanu: kuti tshimene tshomwe
tshiri tshotalitsidwa mwa antu tshiri tshonyansa m' kuona
kwa Mulungu. Mau ndi aprofeti *zinali* kwa Yohane: kwa 16
ntawi imene ivangeli wa dziko la Mulungu uuzidwa, ndi
antu onse atitimiza mwa ilo. Koma tshiri tshopepuka kwa 17
kumwamba ndi dziko ku pita, tshopambana kwa kakang'ono
kamodzi ka mau ku gwa. Iemwe atshotsa nkazi watshi, 18
nakwata wina, atshita tshigololo: ndimo iemwe akwata
modzi emwe atshotsedwa kwa mamuna atshita tshigololo.

Ndimo kunali muntu modzi wolemera, ndimo nabvala 19
yakuda ndi nsaru ya lini yabwino, kudia zabwino masiku
onse: ndimo muntu modzi wosauka atshedwa Lazaro 20
naikidwa pa tshipata tshatshi, wodzaza ndi zironda, ndimo 21
kufuna ku etedwa ndi *nyenyeswa* zomwe zinagwa kwa gome
la muntu wolemera; koma inde agaru nadza naseteka
zironda zatshi. Ndimo kunali, kuti wosauka nafa, ndimo 22
kuti nanyamulidwa ndi anjelo m' tshifua tsha Abraham:
ndimo muntu wolemera anso nafa, naikidwa m' mwanda.
Ndimo mwa Hadesi natukula maso atshi, anali ndi masautso, 23

ndimo aona Abraham kutali, ndi Lazaro m' tshifua tshatshi.
24 Ndimo napfula nati, Atate Abraham, kala ndi nsisi ndi ine,
nutumize Lazaro, kuti angobiza nsonga ya tshala tshatshi m'
madzi, naziziritsa lilume langa; kuti dipwetekwa m' lilume
25 la moto limene. Koma Abraham nati, Mwana, kumbukila
kuti iwe m' moyo wako unalandira zintu zako zabwino,
ndimo onso Lazaro zintu zoipa: koma tsopano kuno
26 asangalatsidwa, ndimo upwetekwa. Ndimo opambana zonse
zimene, pakati pa ife ndi inu, liripo phompo lalikuru
loikidwa: kuti awo omwe afuna ku pita kuno kwa inu
osadziwa, ndi kuti palibe angoyambuka kwa uko kwa ife.
27 Ndimo nati, Ndimo dipempera iwe, atate, kuti ukatumiza ie
28 ku nyumba ya atatu anga; kuti diri ndi abali asanu; kuti
angomariza ndi awo, kani awo onso afika m' malo amene a
29 kupwetekwa. Koma Abraham anena, Ali ndi Moses ndi
30 aprofeti; angomvera awo. Ndimo nati, Iai, atate Abraham:
koma ngati modzi ang'ka nao kwa akufa, adzatembenuza
31 mitima yao. Ndimo nanena nai', Ngati osamvera Moses ndi
aprofeti, kapena osadzakantshiziridwa, ngati modzi auka
kwa akufa.

17 Ndimo nanena ndi akupunzira atshi, Kuli kusata koma
kuti makwiitso akadza: koma tshaipa kwa ie, mwa emwe
2 adza! Tshiri tshabwino kwa ie ngati mpero imangidwa pa
kosi latshi, ndimo aponyedwa m' nyanja, tshopambana kuti
3 ie akapuntwitsa modzi wa timene tating'ono. Yang'anirani
inu noka: ngati mpwako atshimwa, dzudzula ie; ndimo
4 ngati atembenuza ntima watshi, kululukira ie. Ndimo
ngati atshimwa pa iwe kasanu ndi kawiri m' dzua, ndi
kasanu ndi kawiri abwera kwa iwe, kuti, ditembenuza
ntima wanga; udzakululukira ie.

5 Ndimo apostile nanena ndi Mwini, Kulitsa mvanu watu.
6 Ndimo Mwini nati, Ngati muli ndi mvanu monga ndi
mpetshe ya mostade, mukanena ndi ntengo wa sikamine
umene, Zulidwa ndi mitsitsi, ndimo uokedwe m' nyanja;
7 ndimo ukanamvera inu. Koma ndani ali wa inu, ali ndi
kapolo kukusa kapena kubusa, emwe adzanena ndi ie, ntawi
anabwera ku munda, Idza tsopano lino nukala pansi pa
8 kudia; ndimo wosadzanena kopambana nai', Konzetsa
tshomwe dingodia, nudzimangitsa, nuimirira ine, kwa ntawi
dadia ndamwa; ndimo pambuiu udzadia nudzamwa?
9 Kodi ayamika kapolo tshifuka natshita zintu zomwe
10 zinauzidwa? Inde tshointsho inu unso, ntawi mwatshita

zintu zonse zomwe ziuzidwa kwa inu, nenani, Tiri akapolo
osapindula: tatshita tshimene tshomwe tshinali ntshito yatu
ku tshita.

Ndimo kunali, monga analikuenda ku Yerusalem, kuti 11
analikupita pakati pa Samariya ndi Galileya. Ndimo monga 12
naloa m' mudzi umodzi, nakomana nai', antu kumi omwe
anali akate, omwe naima kutali: ndimo natukula mau ao, 13
kuti, Yesu, Ambuiye, kala ndi nsisi ndi ife. Ndimo ntawi 14
naona awo, nanena nao, Endani mudzisonyeza ku adzukuru.
Ndimo kunali, monga analikupita, anatsukidwa. Ndimo 15
modzi wa awo, ntawi naona kuti anatshiritsidwa, nabwera,
ndi liu lalikuru kupambanitsa Mulungu; ndimo nagwa ndi 16
nkope yatshi pa mapazi atshi, kunena tshakoma kwa ie:
ndimo anali Msamariya. Ndimo Yesu kuiang'ka nati, Kodi 17
sanali kumi otsukidwa? koma asanu ndi anai ali kuti?
Kodi sanapezedwa omwe nabwera ku patsa kupambana kwa 18
Mulungu, koma mlendo amene? Ndimo nanena nai', Uka, 19
muka: mvanu wako wakutshiritsa.

Ndimo ntawi anafunsidwa ndi Afarisi, ntawi dziko la 20
Mulungu lidza, naiang'ka awo nati, Dziko la Mulungu
losadza ndi kuyang'anira: kapena osadzanena, Ona, pano! 21
kapena, Apo! kuti ona, dziko la Mulungu liri mwa inu.

Ndimo nanena ndi akupunzira, Masiku adzafika, ntawi 22
mudzafuna ku ona limodzi la masiku a Mwana wa muntu,
ndimo simudzaliona. Ndimo adzanena ndi inu, Ona, apo! 23
Ona, pano! musatshoka, kapena musatsata pambuiu *awo:*
kuti monga mpezi, ntawi iwalima kwa malo a modzi pansi 24
pa kumwamba, iwala ku malo ena pansi pa kumwamba;
tshointsho Mwana wa muntu adzakala m' dzua latshi.
Koma patsogolo akanamva zintu zambiri nakanidwa ndi fuko 25
limene. Ndimo monga kunali m' masiku a Nowa, inde 26
tshointsho tshidzakala anso m' masiku a Mwana wa muntu.
Nadia, namwa, nakwata, napatsidwa ku kwatibwa, kwa dzua 27
lomwe Nowa naloa m' arke, ndimo tshigumula tshinafika,
ndimo tshinamwaza awo onse. Tshointsho inde monga 28
kunali m' masiku a Lote; nadia, namwa, nagula, nagulitsa,
naoka, namanga; koma m' dzua lomwe Lote naturuka kwa 29
Sodom kunabvumba moto ndi sulfere ku mwamba,
namwaza awo onse: tshointsho tshidzakala m' dzua lomwe 30
Mwana wa muntu asonyezedwa. M' dzua limene, iemwe 31
adzakala pamwamba pa nyumba, ndi zintu zatshi m' nyumba,
letsa ie ku tsika ku tenga izo: ndimo iemwe ali m' munda

32 letsa ie enso ku bwera. Kumbukila nkazi wa Lote.
33 Iemwe adzafuna ku pulumutsa moyo watshi adzaumwaza:
koma iemwe adzamwaza *moyo watshi* adzaupulumutsa.
34 Dinena ndi inu, m' siku limene kudzakala antu awiri pa
mpasa imodzi; modzi adzatengedwa, ndi wina adzasiidwa.
35 Kudzakala akazi awiri ku pera pa mpero imodzi; modzi
37 adzatengedwa, ndi wina adzasiidwa. Ndimo awo kuiang'ka
anena nai', Kuti, Mwini? Ndimo nanena nao, Pomwe
ntembo *ulipo*, pomwe miimba anso idzasong'kanidwa.
18 Ndimo nanena fanizo ndi awo monga kuti akanapempera
2 ntawi yonse, ndimo si ku foka; kuti, Muzinda umodzi
kunali woweruza, emwe sanaopa Mulungu, ndimo sanaganiza
3 ndi muntu: ndimo kunali wamasie muzinda umene; ndimo
nadza kawiri kawiri ku ie, kuti, Zimbula ine pa liwongo langa.
4 Ndimo kwa ntawi nakana: koma pambuiu nanena ndi ntima
watshi, Ngati sindiopa Mulungu, kapena sindiganiza ndi
5 muntu; kosuntira tshifuka kuti wamasie amene andivuta,
didzazimbula ie, kani andilemetsa ndi kufika kwatshi kawiri
6 kawiri. Ndimo Mwini nati, Imvani tshomwe woweruza
7 wosadeka ati. Ndimo kodi Mulungu sadzazimbula osang'ki-
dwa atshi, omwe napfula kwa ie msana ndi usiku, ndimo
8 alekereza awo? Dinena ndi inu, kuti adzazimbula awo
nsanga. Koma ntawi Mwana wa muntu afika, kodi
adzapeza mvanu pa dziko?
9 Ndimo nanena anso fanizo limene kwa ena omwe namvana
10 mwa iwo oka kuti anali odeka, nanyoza ena: Antu awiri
nakwera ku tempile ku pempera; modzi Mfarisi, ndi wina
11 wolandira tsong'ko. Mfarisi naima napempera tshointshi
ndi ntima watshi, Mulungu, dinena tshakoma kwa iwe, kuti
sindiri wofana ndi antu ena, oawanya, osadeka, atshigololo,
kapena inde monga wofana ndi wolandira tsong'ko amene.
12 Dikala ndi njala kawiri pa wiki; dipatsa mpambu ya zonse
13 zomwe dilandira. Koma wolandira tsong'ko, kuima kutali,
sanafuna ku tukula inde maso atshi ku mwamba, koma
namenya pa ntima patshi, kuti, Mulungu, kala ndi nsisi ndi
14 ine wampulupulu. Dinena ndi inu, Muntu amene natsika
ku nyumba yatshi wodeketsedwa wopambana wina: kuti
iemwe adzikulitsa adzatshepetsedwa; koma iemwe adzitshe-
petsa adzakulitsidwa.
15 Ndimo natenga anso kwa ie makanda ao, kuti akatosa
awo: koma ntawi akupunzira naona, nasulumula awo.
16 Koma Yesu naitana awo kwa ie, kuti, Rekani tiana ku dza

kwa ine, ndimo musaletsa ito: kuti kwa totere liri dziko la
Mulungu. Dinena ndi inu nditu, Emwe sadzalandira dziko 17
la Mulungu monga kamwana, sadzaloa nditu umo.

Ndimo woweruza modzi namfunsa, kuti, Mpunzitsi wa- 18
bwino, didzatshita tshiani ku loa m' moyo wosamariza?
Ndimo Yesu nanena nai', Bwanje utsha ine wabwino? 19
palibe modzi wabwino kani modzi eka, *inde* Mulungu.
Udziwa mau, Usatshita tshigololo, Usapa, Usaba, Usasinji- 20
rira, Lemekeza atatu ako ndi amai *ako.* Ndimo nati, 21
Zintu zonse zimene dasunga kwa ntawi ya ubwana wanga.
Ndimo ntawi Yesu anamva, nanena nai', Tshintu tshimodzi 22
ulibe kosuntira: gulitsa zonse zomwe uli nazo, nugawa kwa
osauka, ndimo udzali ndi kulemera m' mwamba: nudza,
nunditsata. Koma ntawi anamva zintu zimenezi, anamva 23
tshisoni tshambiri; kuti analemera kwambiri. Ndimo Yesu 24
kumona nati, Bwanje kolimba omwe ali ndi zolemera adza-
loa m' dziko la Mulungu! Kuti kuli kopepuka kwa gamila 25
ku pisa diso la singano kopambana kwa muntu wolemera
ku loa m' dziko la Mulungu. Ndimo awo omwe anamva 26
nati, Ndimo ndani adziwa ku pulumutsidwa? Koma nati, 27
Zintu zomwe ziri zosata ndi antu ziri zakuta ndi Mulungu.
Ndimo Petros nati, Ona, tasia zatu, ndimo tinatsata iwe. 28
Ndimo nanena nao, Dinena ndi inu nditu, Palibe muntu 29
emwe wasia nyumba, kapena nkazi, kapena abali, kapena
atatu atshi ndi amai atshi, kapena ana, kwa dziko la
Mulungu, emwe wosadzalandira kwambiri kopambana mwa 30
ntawi imene, ndi m' kugonera kulinkudza moyo wosamariza.

Ndimo natenga kwa ie kumi ndi awiri, nanena nao, Ona, 31
tikwera ku Yerusalem, ndi zintu zonse zomwe zilembedwa
mwa aprofeti zidzadzazidwa kwa Mwana wa muntu. Kuti 32
adzaperekedwa kwa Mitundu, ndimo adzatsanzidwa, ndi ku
nyozedwa, ndi ku tsiridwa mate: ndimo adzamkwapula 33
ndimo adzampa: ndimo siku latshitatu adzauka anso.
Ndimo nadziwa palibe tshimodzi tsha zintu zimenezi; ndimo 34
kunena kumene kunabisidwa kwa awo, ndimo sanadziwitsa
zintu zomwe zinanenedwa.

Ndimo kunali, monga nayandika ndi Yeriko, muntu 35
modzi wakungu nakala mbali mwa njira kupempa: ndimo 36
kumva antu ambiri kupita, nafunsa tshimene tshinatantauza
bwanje. Ndimo nauza ie, kuti Yesu wa Nazarete aliku- 37
pita. Ndimo napfula, kuti, Yesu, iwe mwana wa Davide, 38
kala ndi nsisi ndi ine. Ndimo awo omwe anapita patsogolo 39

nasulumula ie, kuti akatontola: koma napfula kwambiri
kopambana, Iwe mwana wa Davide, kala ndi nsisi ndi
40 ine. Ndimo Yesu naima, nauza ie ku tengedwa kwa ie:
ndimo ntawi nayandika namfunsa, Ufuna tshiani kuti
41 ditshite ndi iwe? Ndimo nati, Mwini, kuti dione.
42 Ndimo Yesu nanena nai', Ona: mvanu wako wapulumutsa
43 iwe. Ndimo tsopano lino naona, namtsata, kupambanitsa
Mulungu: ndi antu onse, ntawi naona, nalemekeza
Mulungu.

19 Ndimo naloa ndimo analikupita mwa Yeriko. Ndimo
ona, muntu atshedwa Zakeyu; ndimo anali watsong'ko
3 wang'kuru, ndimo anali wolemera. Ndimo nafuna ku
ona Yesu anali ani; ndimo sanadziwa tshifuka tsha antu
4 ambiri, tshifuka anali wa nsing'ku waung'ono. Ndimo
natamanga patsogolo, nakwera pa ntengo wa nkuyu kumo-
5 na: kuti anali ku pita pa njira imene. Ndimo ntawi Yesu
nafika pa malo, nayang'ana kumwamba, nanena nai',
Zakeyu, nsanga, tsika; kuti lero dikanakala pa nyumba
6 yako. Ndimo nsanga natsika, nalandira ie kosekera.
7 Ndimo ntawi anaona, nandandaulira onse, kuti, Analoa
8 ku kala ndi muntu emwe ali wampulupulu. Ndimo
Zakeyu naima, nanena ndi Mwini, Ona, Mwini, nusu la
zintu zanga dipatsa ku osauka; ndimo ngati daawanya
9 kantu kwa muntu modzi, dibweza kanai. Ndimo Yesu
nanena nai', Lero kupulumutsa kunafika ku nyumba imene,
kuti monga ambiri monga ali inso mwana wa Abraham.
10 Kuti Mwana wa muntu nafika ku saka ndi ku pulumutsa
womwazika.

11 Ndimo monga anamva zintu zimenezi, naong'khetsa
nanena fanizo, tshifuka anali pafupi ndi Yerusalem, ndimo
*tshifuka* naganizaganiza kuti dziko la Mulungu linalikuso-
12 nyeza tsopano lino. Ndimo nanena, Wotshuka modzi napita
ku dziko lakutali, ku landira kwa ie eka dziko, ndimo ku
13 bwera. Ndimo naitana akapolo atshi kumi, napatsa awo
mina kumi, nanena nao, Gulitsani *ndi zimene* kwa ntawi
14 difika. Koma antu atshi nakwiira ie, natumiza mitenga
pambuiu pa ie, kuti, Sitifuna kuti muntu amene aweruze
15 ife. Ndimo kunali, ntawi anabwera, analandira dziko, kuti
nauza akapolo amene, kwa omwe anapatsa ndrama, ku
itanidwa kwa ie, kuti anangodziwa tshomwe anapindula ndi
16 kugulitsa. Ndimo woiamba nadza patsogolo pa ie, kuti,
17 Mwini, mina yako inapanga mina kumi zopambana. Ndimo

nanena nai', Tshabwino, iwe kapolo wabwino: tshifuka
unapezedwa ndi mvanu ndi kakang'ono, kala ndi mpamvu
pa mizinda kumi. Ndimo watshiwiri nadza, kuti, Mina 18
yako, Mwini, inapanga mina zisanu. Ndimo nanena nai' 19
inso, Kala iwe enso pa mizinda isanu. Ndimo wina nadza, 20
kuti, Mwini, ona, mina yako *si i*, yomwe dinasunga inaiki-
dwa m' mrenzo: kuti dinaopa iwe, tshifuka uli muntu 21
wokwiakwia: utenga tshomwe usanaika pansi, nutema
tshomwe usanafesa. Anena nai', Kwa nkamwa mwako 22
didzaweruza iwe, kapolo woipa iwe. Unadziwa kuti diri
muntu wokwiakwia, kutenga tshomwe sindinaika pansi, ndi
kutema tshomwe sindinafesa; ndimo bwanje usanaika 23
ndrama zanga m' banke ndimo ine pa kufika kwanga
dikanafuna iyo ndi kupindula? Ndimo nanena nao omwe 24
naima pafupi, Tshotsani kwa ie mina, muipatse kwa emwe
ali ndi mina kumi. Ndimo nanena nai', Mwini, ali ndi 25
mina kumi. Dinena ndi inu, kuti kwa onse apotshera 26
adzapatsidwa; koma kwa emwe sanapotshera, inde tshimene
tshomwe ali natsho tshidzatshotsedwa kwa ie. Koma awa 27
maliwongo anga, omwe sanafuna kuti dikaweruza awo,
tengani kuno, mupa awo patsogolo pa ine.

Ndimo ntawi ananena tshointsho, napita patsogolo, 28
kukwera ku Yerusalem.

Ndimo kunali, ntawi nayandika ndi Betefage ndi 29
Betaniya, pa piri lomwe litshedwa *piri* la Maolive, natumiza
awiri a akupunzira, kuti, Mukani ku mudzi pandunji pa 30
*inu;* momwe monga muloa mudzapeza mwana wa buru
womangidwa, pomwe palibe muntu nakala kosuntira:
masulani ie, mumtenga. Ndimo ngati modzi afunsa inu, 31
Bwanje mumasula ie? mudzanena tshointsho, Mwini ali ndi
kufunidwa ndi ie. Ndimo awo omwe anatumidwa namuka, 32
napeza inde monga ananena nao. Ndimo monga analiku- 33
masula mwana wa buru, eni atshi nanena nao, Bwanje
mumasula mwana wa buru? Ndimo nati, Mwini ali ndi 34
kufunidwa ndi ie. Ndimo namtenga kwa Yesu: ndimo 35
naponya miinjiro yao pa mwana wa buru, naika Yesu pa ie.
Ndimo monga analikupita, nayala miinjiro yao pa njira. 36
Ndimo monga tsopano analikuyandika, *inde* pa kutsika pa 37
piri la Maolive, antu onse ambiri a akupunzira naamba ku
sekera ndi ku lemekeza Mulungu ndi liu lalikuru kwa
mpamvu zonse zomwe anaziona; kuti, Yodala *iri* Fumu 38
Yotshuka yomwe ifika m' dzina la Mwini: ntendere m'

39 mwamba, ndi kupambana mopambanitsa. Ndimo ena a
Afarisi kwa antu ambiri nanena nai', Mpunzitsi, sulumula
40 akupunzira ako. Ndimo naiang'ka nanena, Dikuuza kuti,
ngati amene adzatontola, miala idzapfula.
41 Ndimo ntawi nayandika, naona mzinda nalirira iwo,
42 kuti, Ngati unadziwa mwa siku limene, inde iwe, zintu zo-
mwe ziri za ntendere! koma tsopano zibisidwa kwa maso ako.
43 Kuti masiku adzafika pa iwe, ntawi maliwongo ako adza-
panga linga pa iwe, ndimo adzazunguniza iwe, ndimo
44 adzasunga iwe pa makundu onse, ndimo adzaponya iwe
pansi, ndi ana ako mwa iwe; ndimo sadzaleka mwa iwe
mwala umodzi pa mwala wina; tshifuka kuti sunadziwa
ntawi ya kuyang'anira kwako.
45 Ndimo naloa m' tempile, naamba ku turutsa awo omwe
46 nagulitsa, kunena nao, Alembedwa, Ndimo nyumba yanga
idzakala nyumba ya kupempera: koma munapanga iyo
panga la olanda.
47 Ndimo analikupunzitsa masiku onse m' tempile. Koma
adzukuru akuru ndi akulembera ndi akuru a antu nafuna
48 ku mwaza ie: ndimo sanadziwa ku peza tshomwe anango-
tshita; kuti antu onse nakala pafupi ndi ie, kumvetsa.
20 Ndimo kunali, pa limodzi la masiku, monga analiku-
punzitsa antu m' tempile, ndi kuuza ivangeli, nafika pa ie
2 adzukuru akuru ndi akulembera ndi akuru; ndimo nati,
kunena nai', Uza ife: Ndi mpamvu yanje utshita zintu
zimenezi? kapena ndani ali iemwe anapatsa iwe mpamvu
3 imene? Ndimo naiang'ka nanena nao, Ine enso didzafunsa
4 inu mau; ndimo yang'kani ine: Mbapatisma la Yohane,
5 kodi linali kwa kumwamba, kapena kwa antu? Ndimo
nauzana iwo oka, kuti, Ngati tidzanena, Kwa kumwamba;
6 adzati, Bwanje musanamvana ndi ie? Koma ngati tidzati,
Kwa antu; antu onse adzaponya miala pa ife: kuti
7 akantshiziridwa kuti Yohane anali mprofeti. Ndimo
8 naiang'ka, kuti sanadziwa kuti *linali.* Ndimo Yesu nanena
nao, Kapena sindiuza inu ndi mpamvu yanje ditshita zintu
zimenezi.
9 Ndimo naamba ku nena ndi antu fanizo limene: Muntu
naoka munda wa mvina, naubwereka ku antu otshita m'
10 munda, namuka kwa dziko lina kwa ntawi yeitali. Ndimo
pa nsiku natumiza kapolo kwa antu otshita m' munda, kuti
akapatsa ie kwa dzobala dza munda wa mvina: koma
11 otshita m' munda nanmenya, natumiza ie tshabe. Ndimo

natumiza kosuntira kapolo wina: ndimo ie enso namenya,
natshita ndi ie zoipa, natumiza ie tshabe. Ndimo natumiza 12
kosuntira watshitatu: ndi ie enso nalasa, namturutsa.
Ndimo mwini wa munda wa mvina nati, Didzatshita tshiani? 13
didzatumiza mwana wanga wondikonda: kungokala adza-
lemekeza ie. Koma ntawi otshita m' munda naona ie, 14
nauzana awo oka, kuti, Amene ali woloa: timpe, kuti kuloa
kungokala kwatu. Ndimo anaturutsa ie m' munda wa 15
mvina, nampa. Ndimo tshiani mwini wa munda wa mvina
adzatshita nao? Adzadza nadzamwaza otshita m' munda 16
amene, ndimo adzapatsa munda wa mvina kwa ena. Ndimo
ntawi anamva, nati, Si tshointsho. Koma nayang'ana pao, 17
nati, Ndimo tshiani tshiri tshimene tshomwe tshilembedwa,

Mwala womwe amanga nataia,
Umeneu unapangidwa mutu wa ngondia?

Onse omwe agwa pa mwala umene adzatsholedwa; koma pa 18
emwe udzagwa, udzanyenya ie monga fumbi.

Ndimo akulembera ndi adzukuru akuru nafuna ku ika 19
manja pa ie mwa ora limeneli; ndimo naopa antu: kuti
nadziwitsa kuti ananena fanizo limene pa awo. Ndimo 20
nadikira ie, natumiza zinzondi, zomwe zinadzinyenga ngati
zinali zodeka, kuti zinangogwira mau atshi, monga kuti
adzampereka kwa kuweruza ndi mpamvu za mbiri. Ndimo 21
nafunsa ie, kuti, Mpunzitsi, tidziwa kuti unena nupunzitsa
bwino, ndimo usalandira tupi *la modzi*, koma wa nteradi
upunzitsa njira ya Mulungu: Kodi tshiri tshamau kwa ife 22
ku patsa tsong'ko ku Kesare, kapena iai? Koma nadziwitsa 23
kutshenjera kwao, nanena nao, Sonyeza ine denariyon. 24
Fanizo ndi mlemba za ani linali nazo? Ndimo nanena, Za
Kesare. Ndimo nanena nao, Ndimo patsani kwa Kesare zintu 25
zomwe ziri za Kesare, ndi kwa Mulungu zintu zomwe ziri
za Mulungu. Ndimo sanadziwa ku gwira kunena patsogolo 26
pa antu: ndimo nazizwa ndi kuiang'ka kwatshi, nakala tshete.

Ndimo nafika kwa ie ena a Asadusi, awo omwe anena 27
kuti kuukirira anso palibe; ndimo nafunsa ie, kuti, Mpunzitsi, 28
Moses nalemba kwa ife, kuti ngati njiratshi wa muntu afa,
ali ndi nkazi, ndimo ali wopanda mwana, mpwatshi akatenga
nkazi, nakaukitsa mbeu kwa njiratshi. Ndimo anali abali 29
asanu ndi awiri: ndimo woiamba natenga nkazi, nafa
wopanda mwana: ndimo watshiwiri; ndimo watshitatu 30, 31
natenga ie; ndimo modzimodzi asanu ndi awiri inso sanasia
ana, nafa. Pambuiu nkazi nafa anso. Ndimo m' kuukirira 32, 33

adzakala nkazi waani wa awo? kuti asanu ndi awiri
34 anakwata ie. Ndimo Yesu nanena nao, Ana amamuna a
35 kugonera kumene akwata, nakwatitswa: koma awo omwe
aganizidwa oenera ku fika ku kugonera kudya, ndi kuuki-
rira kwa akufa, kapena osakwata, kapena osakwatitswa:
36 kuti kapena osadziwa ku fa anso: kuti ali amodzimodzi ndi
anjelo; ndimo ali ana amamuna a Mulungu, ali ana a
37 kuukirira. Koma kuti akufa aukitswa, inde Moses naso-
nyeza, m' *malo ndi* Tshifutu, ntawi atsha Mwini Mulungu wa
Abraham, ndi Mulungu wa Yisake, ndi Mulungu wa
38 Yakobi. Ndimo wosali Mulungu wa akufa, koma wa
39 amoyo: kuti onse akala ndi moyo kwa ie. Ndimo ena a
akulembera kuiang'ka nati, Mpunzitsi, wanena bwino.
40 Kuti sanadziwa anso ku funsa ie funso lina.
41 Ndimo nanena nao, Bwanje anena kuti Kristu ali mwana
42 wa Davide? Kuti Davide eka anena m' buku la Masalmo,
Mwini nanena ndi Mwini wanga,
Kala pa dzanja lamanja langa,
43 Kwa ntawi dipanga maliwongo ako mpando wa mapazi
ako.
44 Ndimo Davide atsha ie Mwini, ndimo bwanje ali mwana
watshi?
45 Ndimo m' kumva kwa antu onse nanena ndi akupunzira
46 atshi, Tshenjerani ndi akulembera, omwe afuna ku endaenda
m' miinjiro yeitali, nakonda mautso m' malo a maronda, ndi
mipando yopambana m' masinagoge, ndi malo opambana pa
47 kudia; omwe amwaza nyumba za amasie, ndimo kwa tshi-
nyengo apanga mapempero atali: amene adzalandira
kusutsa kopambana.
21 Ndimo nayang'ana kumwamba, naona antu olemera
2 omwe analikuponya zolere zao m' bokosi la ndrama. Ndimo
naona wamasie modzi wosauka kuponya umo timite tiwiri.
3 Ndimo nanena, Ndi nteradi dinena ndi inu, Wamasie amene
4 wosauka waponya umo wopambana onse: kuti onse amene
kwa kwambiri kwao naponya kwa zolere: koma ie kwa
kusauka kwatshi naponya moyo wonse womwe ali nawo.
5 Ndimo monga ena nanena ndi tempile, bwanje linakonze-
6 tsedwa ndi miala yabwino ndi zolere, nati, Monga ndi zintu
zimenezi zomwe muona, masiku adzadza, mwa amene usa-
dzasiidwa pano mwala umodzi pa wina, womwe usadzapo-
7 nyedwa. Ndimo nafunsa ie, kuti, Mpunzitsi, ndimo zintu
zimenezi zidzafika liti? ndimo tshizindikilo *tshidzali* tshiani

pa ntawi zintu zimene zidzakala? Ndimo nati, Yang'ani- 8
rani kuti musasotsheretswa: kuti ambiri adzafika m' dzina
langa, kuti, Diri *ie;* ndimo, Ntawi iyandika: musapita
pambuiu pao. Ndimo ntawi mudzamva ndi zinkondo ndi 9
mapokoso, musaopa: kuti zintu zimenezi zikanafika patso-
golo; koma nsonga yosali tsopano lino.

Ndimo nanena nao, Mtundu udzauka pa mtundu, ndi 10
dziko pa dziko: ndimo zidzali zibvomezi zazikuru, ndi 11
m' malo ena zinjala ndi dzaola; ndimo zidzali dzoopsa ndi
zizindikilo zazikuru kwa kumwamba. Koma patsogolo pa 12
zintu zonse zimene, adzaika manja ao pa inu, nadzazunza
inu, kupereka inu kwa masinagoge ndi nyumba za ndima,
kutsogoza inu patsogolo mafumu otshuka ndi oweruza kwa
dzina langa. Tshidzatembenuka kwa inu kwa kumariza. 13
Ndimo mueteka mwa mitima yanu, si ku ganizaganiza 14
patsogolo bwanje ku yang'ka: kuti didzapatsa inu nkamwa 15
ndi nzeru, zomwe mariwongo onse anu siadzadziwa ku
kaniza kapena ku nena iai. Koma mudzaperekedwa inde 16
ndi atatu *anu* ndi amai *anu*, ndi abali, ndi omwe a fuko
*lanu* ndi abwenzi; ndi *ena* a inu adzapanga ku pedwa.
Ndimo mudzakwiiridwa ndi antu onse kwa dzina langa. 17
Ndimo palibe tsisi limodzi la mutu wanu lidzamwazika. 18
Mwa kulongosola kwanu mudzapeza mizimu yanu. 19

Koma ntawi muona Yerusalem wozunguliridwa ndi 20
magulu a ankhondo, ndimo dziwani kuti bwinja latshi liri
pafupi. Pomwe awo omwe ali m' Yudeya atawire ku 21
mapiri; ndimo awo omwe ali mkati pa iwo aturuke;
ndimo awo omwe ali m' maiko sialoe umo. Kuti amene ali 22
masiku a kuzimbula, kuti zintu zonse zomwe zilembedwa
zingodzazidwa. Tshaipa kwa iwo omwe ali ndi mimba 23
ndimo kwa iwo omwe aamwitsa m' masiku amene! kuti
kudzali zisoni zambiri pa dziko, ndi kukwiira kwa antu
amene. Ndimo adzagwa ndi kukali kwa mpeni wa 24
nkondo, ndimo adzatsogozedwa kwa mikoli kwa mitundu
yonse; ndimo Yerusalem udzaponderezedwa ndi Mitundu,
kwa ntawi za Mitundu zidzadzazidwa. Ndimo kudzali 25
zizindikilo m' dzua ndi m' mwezi ndi m' nyenyezi; ndimo
pa dziko tshisoni tsha mitundu, m' kuganizaganiza kwa kuula
kwa nyanja ndi mafundi; antu kufoka ndi kuopa, ndimo 26
ndi kuyang'anira zintu zomwe zirinkudza pa dziko: kuti
mpamvu za kumwamba zidzantuntumidwa. Ndimo pomwe 27
adzaona Mwana wa muntu kudza muntambo ndi mpamvu

28 ndi kupambana kwakukuru. Koma ntawi zintu zimenezi
ziamba ku kala, yang'anani kumwamba, ndi tukulani mitu
yanu; tshifuka kuti kuombola kwanu kuyandika.
29 Ndimo nanena nao fanizo: Onani ntengo wa nkuyu ndi
30 mitengo yonse: ntawi tsopano ipakutika, muona ndimo
mudziwa wa inu noka kuti dzinja tsopano liri pafupi.
31 Inde tshointsho inu unso, ntawi muona zintu zimenezi
zirikufika, dziwani kuti dziko la Mulungu liri pafupi.
32 Diuena ndi inu nditu, Fuko limene silidzapita, kwa ntawi
33 zintu zonse zitetsedwa. Kumwamba ndi dziko zidzapita:
koma mau anga osadzapita.
34 Koma yang'anirani inu noka, kani kapena mitima yanu
idzadzazidwa zotshuruka ndi mitshedwa, ndi kuledzera, ndi
ntshito za moyo umene, ndimo siku limene lifika pa inu
35 nsanga monga khango: kuti *tshointsho* lidzafika pa onse
36 omwe akala pa dziko lonse. Koma yang'anirani ntawi
zonse, kupempa, kuti mungopambana ku pulumuka zintu
zonse zimenezi zomwe zidzafika, ndimo ku ima patsogolo pa
Mwana wa muntu.
37 Ndimo masiku onse analikupunzitsa m' tempile; ndimo
madzulo onse naturuka, nakala m' piri lomwe litshedwa
38 *piri* la Maolive. Ndimo antu onse nadza mamawa kwa ie
m' tempile, ku mva ie.
22 Tsopano kudia kwa nkate wopanga tshabe kunayandika,
2 komwe kutshedwa Mpasika. Ndimo adzukuru akuru ndi
akulembera nafuna bwanje anangompa; kuti naopa antu.
3 Ndimo Satana naloa m' Yuda iemwe natshedwa Sikariyoti,
4 ali wa kuwerenga kwa kumi ndi awiri. Ndimo namuka,
nalankulana ndi adzukuru akuru ndi akazembe, bwanje
5 anangompereka kwa iwo. Ndimo nasekera, napangana ku
6 patsa ie ndrama. Ndimo nabvomera, nafuna pofatsa ku
pereka ie kwa iwo kopanda pokoso.
7 Ndimo siku la nkate wopanga tshabe linadza, mwa ilo
8 mpasika ukanatsiridwa. Ndimo natumiza Petros ndi
Yohane, kuti, Mukani konzetsani kwa ife mpasika, kuti
9 tingodia. Ndimo nanena nai', Kuti mufuna kuti tikonzetse?
10 Ndimo nanena nao, Ona, ntawi munaloa muzinda, adzako-
mana ndi inu muntu kunyamula mbia ya madzi; tsatani ie
11 m' nyumba momwe aloa. Ndimo mudzanena ndi mwini
wa nyumba, Mpunzitsi anena ndi iwe, Tshipinda tsha
waulendo tshiri kuti, pomwe didzadia mpasika ndi akupu-
12 nzira anga? Ndimo adzasonya inu tshipinda tshatshikuru

tsha kumwamba tsha zintu: apo fotokozani. Ndimo napita, 13
napeza monga ananena nao: ndimo nafotokoza mpasika.
Ndimo ntawi ora linafika, nakala pansi, ndi apostile nai'. 14
Ndimo nanena nao, Ndi kufuna dafuna ku dia mpasika 15
umene ndi inu patsogolo dipwetekwa: kuti dinena ndi inu, 16
sindidzaudia kwa ntawi udzadzazidwa m' dziko la Mulungu.
Ndimo nalandira tshiko, ndimo ntawi anati tshakoma, nati, 17
Tengani tshimene, mugawana mwa inu noka: kuti dinena 18
ndi inu, sindidzamwa kwa tsopano ndi dzobala dza mvina,
kwa ntawi dziko la Mulungu lidzadza. Ndimo natenga 19
nkate, ndimo ntawi ananena tshakoma, nauswa, napatsa ku
awo, kuti, Umene uli tupi langa lomwe lipatsidwa kwa inu:
tshitani tshimene mwa kukumbuka kwa ine. Ndimo tshiko 20
modzimodzi pambuiu ngonero, kuti, Tshiko tshimene tshiri
testamente watsopano m' mwazi wanga, *inde* umene womwe
utsanulidwa kwa inu. Koma ona, Dzanja la emwe azonda 21
ine liri ndi ine pa gome. Kuti Mwana wa muntu apita 22
nditu, monga kwaambiriridwa: koma tshaipa kwa muntu
amene mwa emwe azondedwa! Ndimo naamba ku funsana 23
iwo oka, uti wa awo anali emwe akatshita tshintu tshimene.
Ndimo kunauka anso makani mwa awo uti wa awo 24
aganizidwa ali wopambana. Ndimo nanena nao, Mafumu 25
otshuka a Mitundu atshita umwini pa iwo; ndimo awo
omwe ali ndi kuweruza pa iwo atshedwa Otshitabwino.
Koma musa*dzakala* tshointsho: koma iemwe adzakala 26
wang'kuru wopambana mwa inu, akale monga wang'ono;
ndimo iemwe ali fumu, monga iemwe aimirira. Kuti akala 27
wopambana uti, iemwe akala pa kudia, kapena iemwe
aimirira? kodi si iemwe akala pa kudia? koma diri mwa
inu monga iemwe aimirira. Koma muli awo omwe muna- 28
kalabe ndi ine m' mayeso anga; ndimo diika kwa inu dziko, 29
inde monga Atatu anga naika kwa ine, kuti mungodia ndi 30
ku mwa pa gome langa m' dziko langa; ndimo mudzakala
pa mipando yotshuka kuweruza mafuko kumi ndi awiri a
Sirayeli. Simon, Simon, ona, Satana nafunsa ku potshera 31
iwe kuti anangopeta iwe monga trigu: koma dinapempa 32
kwa iwe, kuti mvanu wako usangoperewera: ndimo iwe,
ntawi unatembenuka anso, limbikitsa abali ako. Ndimo 33
nanena nai', Mwini, ndi iwe data ku enda ku nyumba ya
ndima ndi ku imfa. Koma nati, Dikuuza, Petros, tambala 34
sadzalira dzua limene, kwa ntawi udzakana katatu kuti
udziwa ine.

35 Ndimo nanena nao, Ntawi dinatumiza inu opanda
katumba, ndi tumba, ndi dzikwakwata, kodi munasoa
36 kantu? Ndimo nati, Palibe kantu. Ndimo nanena nao,
Koma tsopano, iemwe ali ndi katumba, akatenge, ndi tumba
anso: ndimo iemwe alibe, adzagulitsa tshopfundira tshatshi,
37 ndimo agule mpeni wa nkondo. Kuti dinena ndi inu,
kuti tshimene tshomwe tshilembedwa tshikanatedwa mwa
ine, Ndimo anawerengedwa ndi ampulupulu: kuti tshimene
38 tshomwe tshiri ndi ine tshiri ndi kuta. Ndimo nati, Mwini,
ona, pano iripo mipeni iwiri ya nkondo. Ndimo nanena
nao, Tshikwana.
39 Ndimo naturuka, napita, monga ntengo watshi unali, ku
40 piri la Maolive; ndi akupunzira namtsata anso. Ndimo
ntawi anali pa malo, nanena nao, Pemperani kuti musaloa m'
41 tshinyengo. Ndimo nasuntidwa kwa awo monga kuponya
42 kwa mwala; nagwada napempera, kuti, Atate, ngati ufuna,
tshotsa tshiko tshimene kwa ine: koma si kufuna kwanga,
43 koma kwako, kutshitidwe. Ndimo nasonyeza kwa ie njelo
44 kwa kumwamba, kulimbikitsa ie. Ndimo kunali m' kusa-
uka napempera kolimba kopambana: ndi tukuta latshi
linali monga madonto akuru a mwazi kugwa pa ntaka.
45 Ndimo ntawi nauka kwa pempero latshi, nafika ku akupu-
46 nzira, napeza awo agona tulo kwa tshisoni, nanena nao,
Bwanje mugona? Ukani, pemperani, kuti musaloa m'
tshinyengo.
47 Ntawi kosuntira analikunena, ona, antu ambiri, ndi
iemwe natshedwa Yuda, modzi wa kumi ndi awiri, napita
patsogolo pao; ndimo nayandika ku Yesu kumsomsona.
48 Koma Yesu nanena nai', Yuda, kodi uzonda Mwana wa
49 muntu ndi kumsomsona? Ndimo ntawi awo omwe anali ndi
ie naona tshomwe tshidzatsata, nanena, Mwini, kodi tidza-
50 menya ndi mpeni wa nkondo? Ndimo modzi wa awo
namenya kapolo wa ndzukuru wang'kuru, nadula kutu
51 latshi lamanja. Koma Yesu naiang'ka nati, Lekani tshime-
52 netshi. Ndimo natosa kutu latshi, natshiritsa ie. Ndimo
Yesu nanena ndi adzukuru akuru, ndi akazembe a tempile,
ndi akuru, omwe anadza pa ie, Kodi munaturuka, monga
53 pa wolanda, ndi mipeni ya nkondo ndi zindodo? Ntawi
dinali masiku onse ndi inu m' tempile, simunaturutsa manja
anu pa ine: koma limene liri ora lanu, ndi mpamvu ya
ndima.
54 Ndimo nagwira ie, natsogoza ie, namtenga ku nyumba

ya ndzukuru wang'kuru. Koma Petros natsata kutali
pambuiu. Ndimo ntawi anakoleza moto pakati pa bwalo, 55
nakala pansi pamodzi, Petros nakala pakati pao. Ndimo 56
kabutu kamodzi kuona ie monga analikukala m' kuunika
*kwa moto*, ndi kuyang'anitsa ie, nati, Muntu amene enso
anali ndi ie. Koma nakana, kuti, Nkazi, sindidziwa ie. 57
Ndimo pambuiu ntawi yeing'ono wina namona, nati, Uli 58
inso *modzi* wa awo. Koma Petros nati, Muntu, sindiri.
Ndimo pambuiu pa ora limodzi wina natshimika, kuti, Wa 59
nteradi muntu amene enso anali ndi ie: kuti ali Mgalileya.
Koma Petros nati, Muntu, sindidziwa tshomwe unena. 60
Ndimo tsopano lino, ntawi analikunena, tambala nalira.
Ndimo Mwini natembenuka, nayang'ana pa Petros. Ndimo 61
Petros nakumbukila mau a Mwini, bwanje kuti nanena nai',
Patsogolo tambala alira lero, udzakana ine katatu. Ndimo 62
naturuka, nalira misozi yambiri.

Ndimo antu omwe nagwira *Yesu* natonza ie, nammenya. 63
Ndimo namanga maso atshi, nafunsa ie, kuti, Losa: ndani 64
ali iemwe wakumenya? Ndimo zintu zambiri zina nanena 65
pa ie, kutukwana ie.

Ndimo monga nsanga monga linali dzua, gulu la akuru 66
a antu linasong'kanidwa, ndi adzukuru akuru, ndi akule-
mbera; ndimo natsogoza ie mwa gulu lao, kuti, Ngati uli 67
Kristu, uza ife. Koma nanena nao, Ngati diuza inu,
musadzamvana: ndimo ngati difunsa *inu*, musadzaiang'ka. 68
Koma kwa tsopano Mwana wa muntu adzakalitswa pa 69
dzanja lamanja la mpamvu ya Mulungu. Ndimo nati onse, 70
Ndimo kodi uli Mwana wa Mulungu? Ndimo nanena nao,
Munena kuti diri. Ndimo nati, Bwanje tifuna kumariza 71
kwina? kuti ife toka tamva kwa nkamwa mwatshi.

Ndimo gulu lonse la iwo linauka, natsogoza ie patsogolo 23
pa Pilato. Ndimo naamba ku tshula ie, kuti, Tinapeza 2
muntu uyu kutembenuza mtundu watu, nalikuletsa ku
patsa tsong'ko ku Kesare, ndi kunena kuti ie eka ali Kristu,
fumu yotshuka. Ndimo Pilato nafunsa ie kuti, Kodi uli 3
Fumu Yotshuka ya Ayuda? Ndimo naiang'ka ie nati,
Unena. Ndimo Pilato nanena ndi adzukuru akuru ndi 4
antu ambiri, Dipeza palibe tshimo m' muntu amene. Koma 5
anali ndi kufulumiza kopambana, kuti, Afulumiza antu,
kupunzitsa mwa Yudeya lonse, ndi kuamba kwa Galileya
inde ku malo amene. Koma ntawi Pilato anamva, nafunsa 6
ngati muntu ali Mgalileya. Ndimo ntawi nadziwa kuti 7

anali wa malo a kuweruza kwa Herode, namtumiza kwa
Herode, iemwe eka anso anali m' Yerusalem m' masiku
amene.
8 Ndimo ntawi Herode naona Yesu, anasekera kwambiri:
kuti anafuna ku ona ie ntawi yambiri, tshifuka anamva ndi
ie; ndimo nalingalira ku ona tshizindikilo tshina tshina-
9 tshitidwa ndi ie. Ndimo nafunsa ie ndi mau ambiri; koma
10 sanaiang'ka kantu. Ndimo adzukuru akuru ndi akulembera
11 naima, kutshula ie kwambiri. Ndimo Herode ndi ankhondo
atshi namputa, namtonza, ndi kubveka ie ndi mwiinjiro
12 wabwino namtumiza anso ku Pilato. Ndimo dzua lomwe
Herode ndi Pilato napalana bwenzi: kuti patsogolo anali
ndi kukwiirana awa oka.
13 Ndimo Pilato anaitana ku song'kana adzukuru akuru ndi
14 akuweruza ndi antu, nanena nao, Munatenga muntu amene
kwa ine, monga modzi emwe atembenuza antu: ndimo ona,
ine, dinafunsa ie patsogolo pa inu, sindinapeza tshimo mwa
15 muntu amene ndi zintu zimene zomwe mutshulira ie: iai,
kapena si Herode: kuti anatumiza ie enso kwa ife; ndimo ona,
16 palibe kantu koenera kwa imfa katshitidwa ndi ie. Ndimo
18 didzakwapula ie, ndidzamasula ie. Koma napfula onse
pamodzi, kuti, Tshotsa muntu amene, numasula kwa ife
19 Baraba: modzi emwe kwa kupinduka kumene kunapa-
ngidwa muzinda, ndi kwa mbanda, naikidwa m' nyumba
20 ya ndima. Ndimo Pilato nanena nao onso, kufuna ku
21 masula Yesu; koma napfula, kuti, Patshika, patshika ie.
22 Ndimo nanena nao tshitatu, Bwanje, tshimo lanje muntu
amene natshita? sindinapeza tshifukwa tsha imfa mwa ie:
23 ndimo didzamkwapula ndidzamasula ie. Koma anali nsanga
ndi mau akuru, kufunsa kuti anangopatshikidwa. Ndimo
24 mau ao anapambana. Ndimo Pilato natshula kuti tshomwe
25 nafunsira tshikatshitidwa. Ndimo namasula iemwe kwa
kupinduka ndi mbanda anaikidwa m' nyumba ya ndima,
iemwe anafunsira; koma Yesu napereka kwa kufuna
kwao.
26 Ndimo ntawi analikutsogoza ie, nagwira modzi Simon wa
Kirene, kuturuka m' minda, ndimo pa ie naika nkhwitshi,
ku nyamula iyo pambuiu pa Yesu.
27 Ndimo linatsata ie gulu lalikuru la antu, ndi la akazi
28 omwe nalira nakala ndi tshisoni ndi ie. Koma Yesu
kutembenuka kwa iwo nati, Ana akazi a Yerusalem,
musalira kwa ine, koma lirani kwa inu noka. ndi kwa ana

anu. Kuti ona, masıku alinkudza, momwe adzati, Odala 29
ali atshimbwira, ndi zibaliro zonıwe zosanabala, ndi mabere
omwe sanamwitsa. Pomwe adzaamba ku nena ndi mapiri, 30
Igwani pa ife; ndi kwa zintunda, Fundikilani ife. Kuti 31
ngati atshita zintu zimenezi mwa ntengo wowisi, tshidza-
tshitidwa tshiani mwa wouma?

Ndimo anali inso awiri ena, otshitazoipa, natsogozedwa 32
ndi ie ku pedwa.

Ndimo ntawi anafika pa malo pomwe atshedwa Pala, apo 33
anapatshika ie, ndi otshitazoipa, modzi pa dzanja lamanja
ndi wina pa lamanzere. Ndimo Yesu nati, Atate, kululu- 34
kira awo; kuti siadziwa tshomwe atshita. Ndimo kugawa
miinjiro yatshi mwa iwo, nayesa. Ndimo antu naima ku 35
ona. Ndimo oweruza anso namnyansa, kuti, napulumutsa
ena; adzipulumutse, ngati amene ali Kristu wa Mulungu,
wosang'kidwa watshi. Ndimo ankhondo anso namtonza, 36
kudza kwa ie, kupatsa ie vinegre, ndi kuti, Ngati uli Fumu 37
Yotshuka ya Ayuda, udzipulumutse. Ndimo kunali inso 38
lemba pamwamba pa ie, IMENE IRI FUMU YOTSHUKA YA
AYUDA.

Ndimo modzi wa otshitazoipa omwe anapatshikidwa 39
nasinjirira ie, kuti, Kodi suli Kristu? pulumutsa iwe eka
ndi ife. Koma wina naiang'ka, ndi kusulumula ie, nati, 40
Kodi usaopa inde Mulungu, kuona uli m' sautso imodzi-
modzi? Ndi ife nditu kodeka; kuti tilandira malipiro 41
abwino kwa ntshito zatu: koma muntu amene watshita
palibe kantu koipa. Ndimo nanena, Yesu, kumbukila ine 42
ntawi udza m' dziko lako. Ndimo nanena nai', Dinena ndi 43
iwe nditu, Lero udzakala ndi ine m' Paradisi.

Ndimo tsopano kunali pa ora latshisanu ndi tshimodzi, 44
ndimo ndima unadza pa dziko lonse kwa ora latshisanu ndi
tshinai, kuwala kwa dzua kuperewera: ndi tshopimba tsha 45
malo oyera tshinaganikana pakati. Ndimo ntawi Yesu ana- 46
pfula ndi liu lalikuru, nati, Atate, m' manja ako dipatsa
nzimu wanga: ndimo ananena tshimene, natsirizika. Ndimo 47
ntawi kenturione naona tshomwe tshinatshitidwa, napamba-
nitsa Mulungu, kuti, Amene anali muntu wodeka nditu.
Ndimo antu ambiri onse omwe anasong'kana kwa kuona 48
kumene, ntawi naona zintu zomwe zinatshitidwa, nabwera
kumenya pa dzifua dzao. Ndimo anzatshi onse, ndi akazi 49
omwe natsata ie kwa Galileya, naima kutali, kuona zintu
zimenezi.

50 Ndimo ona, muntu atshedwa Yosefe, emwe anali nkoswe,
51 muntu wabwino ndi wodeka (iemwe sanabvomera kwa ku-
weruza ndi ntshito za iwo), *muntu* wa Arimateya, mzinda
wa Ayuda, iemwe analikuyang'anira kwa dziko la Mulungu:
52 muntu amene nang'ka kwa Pilato, nafunsa kwa ntembo wa
53 Yesu. Ndimo nautsitsa, naukuta m' nsaru ya lini, namwika
m' mwanda womwe unafulidwa m' mwala, momwe palibe
54 muntu anagona patsogolo. Ndimo linali siku la Kukonzetsa,
55 ndimo sabata linafika. Ndimo akazi, omwe anadzera ndi
ie kwa Galileya, natsata, naona mwanda, ndi bwanje ntembo
56 watshi unaikidwa. Ndimo nabwera, nakonzetsa zonung'kira
ndi mafuta.

24 Ndimo pa sabata napuma kofana ndi mau. Koma pa
dzua loamba la wiki, banda kutsha, nadza ku mwanda,
2 kutenga zonung'kira zomwe anakonzetsa. Ndimo napeza
3 mwala unagubuduzidwa kwa mwanda. Ndimo naloa, ndimo
4 sanapeza tupi la Mwini Yesu. Ndimo kunali, ntawi anali-
kuganizaganiza ndi tshimene, ona, antu awiri naima pafupi
5 nao mwa nsaru zowala: ndimo monga naopa, nagudama
nkope zao pansi, nanena nao, Mufunanje wamoyo mwa
6 akufa? Sali pano, koma anauka: kumbukilani bwanje
7 nanena ndi inu ntawi anali kosuntira m' Galileya, kunena
kuti Mwana wa muntu akanaperekedwa m' manja a antu oipa,
8 napatshikidwa, ndimo siku latshitatu nauka anso. Ndimo
9 nakumbukila mau atshi, nabwera ku mwanda, nauza zintu
zonse zimenezi kwa kumi ndi modzi, ndi ku onse ena.
10 Ndimo anali Mariya kwa Magadala, ndi Yohana, ndi Mariya
*amai atshi* a Yakobi: ndi akazi ena nao nauza zintu zimenezi
11 kwa apostile. Ndimo mau amene nasonya m' kuona kwao
12 monga kulankula kwatshabe; ndimo sanamvana nao. Koma
Petros nauka, natamanga ku mwanda; ndi kuwerama ndi
kusuzumira, aona nsaru za lini pa zoka; ndimo namuka
kwatshi, kuzizwa ndi tshimene tshomwe tshinali.

13 Ndimo ona, awiri a awo analikuenda dzua lomwe ku
mudzi utshedwa Emaus, womwe unali kwa Yerusalem ma-
14 stadia makumi asanu ndi limodzi. Ndimo analankula awo
15 oka ndi zintu zonse zimene zomwe zinatshitidwa. Ndimo
kunali, ntawi nalankulana nafunsana, kuti Yesu eka nase-
16 ndezera nang'ka nao. Koma maso ao anagwidwa kuti
17 sakadziwa ie. Ndimo nanena nao, Mau anje ali amene omwe
muli modzi ndi wina, monga mupita? Ndimo naima,
18 kuyang'ana ndi tshisoni. Ndimo modzi wa awo, atshedwa

Kleopa, kuiang'ka nanena nai', Kodi uli weka mlendo m'
Yerusalem ndimo usadziwa zintu zomwe zinali apo m'
masiku amenewa? Ndimo nanena nao, Zintu ziti? Ndimo 19
nanena nai', Zintu ndi Yesu wa Nazarete, emwe anali
mprofeti wolimba mwa ntshito ndi m' mau patsogolo
Mulungu ndi antu onse: ndimo bwanje adzukuru akuru 20
ndi akuru atu nampereka ku sutsidwa kwa imfa, napatshika
ie. Koma tinalingalira kuti anali iemwe akaombola Sirayeli. 21
Inde ndi kupambana zonse zimenezi, tsopano liri siku latshi-
tatu kwa ntawi zintu zimenezi zinakala. Inde ndi akazi 22
ena a gulu latu natizizwitswa, omwe anali ku mwanda banda
kutsha; ndimo ntawi sanapeza tupi latshi, nadza, kunena, 23
kuti anaona anso tshoona tsha anjelo, omwe nanena kuti
anali ndi moyo. Ndi ena a omwe anali ndi ife namuka ku 24
mwanda, napeza itsho inde monga akazi ananena: koma ie
sanaona. Ndimo nanena nao, O antu opusa, ndi ododoma a 25
mitima ku mvana pambuiu zonse zomwe aprofeti analankula!
Kodi Kristu akanamva zintu zimenezi, ndi ku loa m' kupa- 26
mbana kwatshi? Ndimo kuamba kwa Moses ndi aprofeti 27
onse, nasandutsa kwa awo m' malemba onse zintu ndi ie eka.
Ndimo nayandika mudzi, pomwe analikupita: ndimo ie 28
natshita monga ngati nafuna ku pitira. Ndimo naumirira 29
ie, kuti, Kala ndi ife: kuti ali madzulo, ndi dzua tsopano
lirikupita patali. Ndimo naloa ku kala nao. Ndimo kunali, 30
ntawi anakala pa kudia nao, natenga nkate, nadalitsa uo,
nauswa, naupatsa ku awo. Ndimo maso ao anatsegulidwa, 31
ndimo nadziwa ie; ndimo ie nakanganuka kwa kuona kwao.
Ndimo nanena modzi ndi wina, Kodi si mitima yatu inali- 32
kupsa mwa ife, ntawi ananena ndi ife m' njira, ntawi
anatsegula kwa ife malemba? Ndimo nauka pa ora lomwe, 33
nabwera kwa Yerusalem, napeza kumi ndi modzi anasong'-
kanidwa, ndi awo omwe anali nao, kuti, Mwini anauka 34
nditu, ndimo wadzisonya ku Simon. Ndimo nauza zintu 35
*zomwe zinatshitidwa* m' njira, ndi bwanje anadziwidwa ndi
awo m' kuswa nkate.

Ndimo monga nanena zintu zimene, ie eka naima pakati 36
pao, ndimo anena nao, Ntendere *ukale* ndi inu. Koma 37
anatshita manta naopa, naganizaganiza kuti anaona nzimu.
Ndimo nanena nao, Muntentemera bwanje? ndi bwanje 38
maganizo auka m' mitima yanu? Onani manja anga ndi 39
mapazi anga, kuti diri ndeka: tosani ine, ndi onani; kuti nzimu
suli ndi nyama ndi mafupa, monga muona diri nazo. Ndimo 40

ntawi ananena tshimene, nasonyeza awo manja atshi ndi
41 mapazi atshi. Ndimo ntawi kosuntira sanamvana ndi
tshimwemwe, nazizwa, nanena nao, Kodi muli ndi kantu
42 ka kudia pano? Ndimo napatsa ie tshipinjiri tsha nsomba
43 yootsha. Ndimo natshitenga, natshidia patsogolo pa awo.
44 Ndimo nanena nao, Amene ali mau anga omwe dinanena
ndi inu, ntawi dinali kosuntira ndi inu, bwanje kuti zintu
zonse zikanadzazidwa, zomwe zilembedwa m' mau a Moses,
45 ndi aprofeti, ndi masalmo, ndi ine. Pomwe natsegula
46 muwongo wao, kuti anangodziwa malemba; ndimo nanena
nao, Tshointshi tshilembedwa, kuti Kristu akamva, ndimo
47 akauka anso kwa akufa siku latshitatu; ndi kuti kute-
mbenuza kwa ntima ndi kubweza kwa zakwaipa zika-
nauzidwa m' dzina latshi kwa mitundu yonse, kuamba
48 kwa Yerusalem. Muli omariza a zintu zimenezi.
49 Ndimo ona, ditumiza lonjezano la Atatu anga pa inu:
koma kalani inu muzinda, kwa ntawi munabvekedwa
ndi mpamvu kwa kumwamba.
50 Ndimo natsogoza awo kwa ntawi *anali* pandunji pa Beta-
51 niya: ndimo natukula manja atshi, nadalitsa awo. Ndimo
kunali, ntawi ie nadalitsa awo, anaganika kwa awo, ndimo
52 ananyamulidwa kumwamba. Ndimo napembedza ie, na-
53 bwera ku Yerusalem ndi tshimwemwe tshatshikuru: ndimo
anali ntawi yonse m' tempile, kudalitsa Mulungu.

---

# IVANGELI WA YOHANE.

1 M' KUAMBA anali Mau, ndi Mau anali ndi Mulungu, ndi
Mau anali Mulungu. Amene anali m' kuamba ndi
3 Mulungu. Zintu zonse zinapangidwa ndi ie; ndimo
kopanda ie kunalibe kantu kanapangidwa komwe kanapangi-
4 dwa. Mwa ie unali moyo; ndi moyo unali kuunika kwa
5 antu. Ndimo kuunika kuwala mudima; ndimo ndima
6 usanadziwitsa. Kunali muntu, watumidwa ndi Mulungu,
7 dzina latshi linali Yohane. Amene nadza kwa kumariza,
monga kuti anangomariza ndi kuunika, monga kuti onse mwa

ie anangomvana. Sanali kuunika kumene, koma *nafika* kuti 8
anangomariza ndi kuunika. Kunali kuunika koona, *inde* 9
*kuunika* komwe kuunikira antu onse, aloa m' dziko. Anali m' 10
dziko, ndi dziko linapangidwa ndi ie, ndi dziko lisanadziwa ie.
Anafika ku antu atshi, ndimo omwe anali antu atshi sana- 11
mlandira. Koma monga ambiri monga analandira ie, ku awa 12
napatsa kwatshi ku kala ana a Mulungu, *inde* ku awa omwe
amvana ndi dzina latshi: omwe anabadwa, si ndi mwazi, 13
kapena si ndi kufuna kwa nyama, kapena si ndi kufuna
kwa muntu, koma kwa Mulungu. Ndimo Mau nakala 14
nyama, nakala mwa ife (ndimo tinaona kupambana kwatshi,
kupambana monga kwa wobadwa eka kwa Atate), wodzaza
ndi kufatsa ndi nteradi. Yohane amariza ndi ie, napfula, 15
kuti, amene anali ie wa iemwe dinanena, Ie emwe adza
pambuiu pa ine wakala patsogolo pa ine: kuti anali
patsogolo pa ine. Kuti kwa kudzaza kwatshi ife tonse 16
tinalandira, ndi kufatsa kwa kufatsa. Kuti mau anapatsidwa 17
ndi Moses; kufatsa ndi nteradi zinadza ndi Yesu Kristu.
Palibe muntu waona Mulungu ntawi ina; Mwana wobadwa 18
eka, iemwe ali m' tshifua tsha Atate, anasonyeza *ie.*

Ndi kumene kuli kumariza kwa Yohane, ntawi Ayuda 19
natumiza kwa ie adzukuru ndi Alevi kwa Yerusalem
kumfunsa, Uli ani? Ndimo nabvomera, sanakana; ndimo 20
nabvomera, Sindiri Kristu. Ndimo namfunsa, Ndimo 21
bwanje? Uli Eliya? Ndimo ati, Sindiri. Uli mprofeti?
Naiang'ka, Iai. Ndimo nanena nai', Uli ani? kuti tingo- 22
patsa bvomero ku omwe anatitumiza. Uti tshiani ndi iwe
eka? Nati, Diri liu la modzi kupfula m' tshipululu, Lunga- 23
mitsani njira ya Mwini, monga nati mprofeti Yesaya. Ndimo 24
anatumidwa kwa Afarisi. Ndimo namfunsa, nanena nai', 25
Ndimo ubapatiza bwanje, ngati usali Kristu, kapena Eliya,
kapena mprofeti? Yohane naiang'ka nao, kuti, Dibapatiza 26
ndi madzi: modzi aima mwa inu iemwe musadziwa, *inde* 27
emwe adza pambuiu pa ine, tshingwe tsha tshikwakwata
tsha iemwe sindiri woenera ku masula. Zintu zimenezi 28
zinatshitidwa m' Betaniya patsidia lidya la Yordan, pomwe
Yohane analikubapatiza.

Mawa aona Yesu kudza kwa ie, nati, Ona, Mwana wa 29
nkosa wa Mulungu, iemwe atshotsa mpulupulu za dziko!
Amene ali ie wa iemwe dinanena, Pambuiu pa ine alinku- 30
dza muntu iemwe wakala patsogolo pa ine: kuti anali
patsogolo pa ine. Ndimo sindadziwa ie; koma kuti 31

akasonyezedwa kwa Sirayeli, kwa tshifukwa tshimene dinadza
32 kubapatiza ndi madzi. Ndimo Yohane namariza, kuti,
Daona Nzimu kutsika monga njiwa ku mwamba; ndimo
33 unakala pa ie. Ndimo sindinamdziwa: koma iemwe
ananditumiza ku bapatiza ndi madzi, nanena ndi ine, Pa
iemwe udzaona Nzimu kutsika, nukala pa ie, iemwe ali
34 ie emwe abapatiza ndi Nzimu Woyera. Ndimo daona,
namariza kuti amene ali Mwana wa Mulungu.
35 Anso mawa Yohane analikuima, ndi awiri a akupunzira
36 atshi; ndimo nayang'ana pa Yesu monga naenda, ndimo ati,
37 Ona, Mwana wa nkosa wa Mulungu! Ndimo akupunzira
38 awiri anamva ie ku lankula, ndimo natsata Yesu. Ndimo
Yesu natembenuka, naona awa kutsata, ndimo anena nao,
Mufuna tshiani? Ndimo nanena nai', Rabi (omwe ali
39 kunena, kusandukidwa, Mpunzitsi), ukala kuti? Anena
nao, Idzani, ndimo mudzaona. Ndimo nadza naona pomwe
nakala; nakala nai' siku limenelo: kunali pa ora kumi.
40 Modzi wa awiri omwe anamva Yohane *ku nena*, natsata ie,
41 anali Andreya, mpwatshi wa Simon Petros. Poiamba apeza
njiratshi Simon, nanena nai', Tapeza Mesiya (omwe ali,
42 kusandukidwa, Kristu). Namtenga kwa Yesu. Yesu
nayang'ana pa ie, nati, Uli Simon mwana wa Yohane:
udzatshedwa Kefa (omwe kusandukidwa, Petros).
43 Mawa nafuna ku turuka ku Galileya, ndimo apeza Filipu:
44 ndimo Yesu anena nai', Tsata ine. Ndimo Filipu anali kwa
45 Betsayida, wa mzinda wa Andreya ndi Petros. Filipu
apeza Natanayeli, nanena nai', Tapeza ie, wa iemwe Moses
m' mau, ndi aprofeti, analemba, Yesu wa Nazarete, mwana
46 wa Yosefe. Ndimo Natanayeli nanena nai,' Kodi kantu
kabwino kadziwa ku turuka kwa Nazarete? Filipu anena
47 nai', Idza uone. Yesu naona Natanayeli kudza kwa ie,
ndimo anena ndi ie, Ona, Msirayeli nditu, mwa emwe palibe
48 tshinyengo! Natanayeli anena nai', Udziwa bwanje ndi
ine? Yesu naiang'ka nanena nai', Patsogolo Filipu nakui-
tana, ntawi unali pa tsindi pa ntengo wa nkuyu, dinakuona.
49 Natanayeli naiang'ka nai', Rabi, uli Mwana wa Mulungu;
50 uli Fumu Yotshuka ya Sirayeli. Yesu naiang'ka nanena
nai', Tshifuka kuti dinanena ndi iwe, Dinakuona pa tsindi
pa ntengo wa nkuyu, umvana kodi? udzaona zintu zazikuru
51 zopambana zimenezi. Ndimo anena nai', Dinena ndi inu
nditu, nditu, Mudzaona mwamba motsegulidwa, ndi anjelo
a Mulungu kukwera ndi kutsika pa Mwana wa muntu.

Ndimo pa siku latshitatu kunali kukwatitsa mwa Kana 2
wa Galileya; ndi amai a Yesu anali apo: ndi Yesu unso 2
anaitanidwa, ndi akupunzira atshi, kwa kukwatitsa. Ndimo 3
ntawi vinyo naperewera, amai a Yesu anena nai', Osapo-
tshera vinyo. Ndimo Yesu anena nai', Nkazi, dirikutshita 4
tshiani ndi iwe? ora langa lisafika tsopano. Amai atshi 5
anena ndi abandazi, Tshomwe anena ndi inu, tshitani.
Ndimo kunaikidwa apo mbia za madzi zisanu ndi imodzi za 6
miala wofana ndi mwambi wa kuyeretsa wa Ayuda, ku-
landira modzimodzi mafirkin awiri kapena atatu. Yesu 7
anena nao, Dzazani mbia za madzi ndi madzi. Nadzaza izo
ku milomo. Ndimo anena nao, Tungani tsopano, nyamulani 8
ku kazembe wa kudia. Nanyamula. Ndimo ntawi ka- 9
zembe wa kudia analawa madzi omwe tsopano anali vinyo,
ndimo sanadziwa kuti anali (koma abandazi omwe anatunga
madzi nadziwa), kazembe wa kudia aitana wokwati, nanena 10
nai', Antu onse pakuamba aika vinyo wabwino; ndimo
ntawi *antu* anamwa ambiri, *pomwe* emwe ali woipa: wasunga
vinyo wabwino kwa tsopano. Tshoiamba tshimene tsha 11
zizindikilo zatshi Yesu natshita m' Kana wa Galileya,
nasonyeza kupambana kwatshi; ndimo akupunzira atshi
anamvana ndi ie.

Pambuiu tshimene natsika ku Kapernahum, ie, ndi amai 12
atshi, ndi abali *atshi*, ndi akupunzira atshi: nakala apo si
masiku ambiri.

Ndimo mpasika wa Ayuda unali pafupi, ndimo Yesu na- 13
kwera ku Yerusalem. Napeza m' tempile awo omwe 14
nagulitsa ng'ombe ndi nkosa ndi njiwa, ndi osintana ndrama
kukala: ndimo napanga nsempere za zingwe zazing'ono, 15
naturutsa onse m' tempile, ndi nkosa ndi ng'ombe; nate-
mbenuza ndrama za osintana, nagwetsa magome ao; nanena 16
ndi omwe nagulitsa njiwa, Tshotsa zimenezi muno; musa-
panga nyumba ya Atatu anga nyumba ya malonda. Aku- 17
punzira atshi nakumbukila kuti analembedwa, Utshitsanzo
wa nyumba yako udzadia ine. Ndimo Ayuda naiang'ka 18
nanena nai', Tshizindikilo tshiani usonyeza kwa ife, tshifuka
kuti utshita zintu zimenezi? Yesu naiang'ka nanena nao, 19
Mwaza malo oyera amene, ndimo m' masiku atatu didza-
aukitsa. Ndimo Ayuda nati, Dzaka makumi anai ndi 20
dzisanu ndi tshimodzi anali malo oyera amene kumangidwa,
ndimo kodi udzaaukitsa m' masiku atatu? Koma nanena 21
ndi malo oyera a tupi latshi. Ndimo ntawi anaukitswa kwa 22

imfa, akupunzira atshi nakumbukila kuti ananena tshimene;
ndimo namvana mlemba, ndi mau omwe Yesu ananena.
23 Ndimo ntawi anali m' Yerusalem pa mpasika, m' ntawi
ya kudia, ambiri namvana m' dzina latshi, kuona zizindikilo
24 zatshi zomwe nazitshita. Koma Yesu sanadzimvana ku
25 awo, tshifuka kuti nadziwa antu onse, ndimo tshifuka kuti
sanafunira kuti modzi akamariza ndi muntu; kuti ie eka
nadziwa tshomwe tshinali m' muntu.

3 Ndimo kunali muntu wa Afarisi, atshedwa Nikodemo,
2 mkuru wa Ayuda: iemwe nadza kwa ie usiku, nanena nai'
Rabi, tidziwa kuti uli mpunzitsi wadzera kwa Mulungu:
kuti palibe muntu adziwa ku tshita zizindikilo zimene
3 zomwe utshita, kani Mulungu ali nai'. Yesu naiang'ka
nanena nai', Dinena ndi iwe nditu, nditu, Ngati muntu
wosabadwa anso, wosadziwa ku ona dziko la Mulungu.
4 Nikodemo anena nai', Bwanje muntu adziwa ku badwa
ntawi ali wang'kuru? kodi adziwa ku loa tshiwiri m'
5 tshibaliro tsha amai atshi, nabadwa? Yesu naiang'ka,
Dinena ndi iwe nditu, nditu, Kani muntu abadwa ndi madzi
ndi Nzimu, wosadziwa ku loa m' dziko la Mulungu.
6 Tshomwe tshibadwa ndi nyama tshiri nyama; ndi tshomwe
7 tshibadwa ndi Nzimu tshiri nzimu. Usazizwa kuti danena
8 ndi iwe, Ukanabadwa anso. Mpepo iomba pomwe ifuna,
ndimo umva liu la iyo, koma usadziwa pomwe idzera, ndi
pomwe ing'ka: tshointsho ali onse omwe abadwa ndi Nzimu.
9 Nikodemo naiang'ka nanena nai', Zintu zimenezi zikala
10 bwanje? Yesu naiang'ka nanena nai', Kodi uli mpunzitsi
11 wa Sirayeli, ndimo usadziwa zintu zimenezi? Dinena ndi
iwe nditu, nditu, Tilankula tshomwe tidziwa, ntimariza ndi
tshomwe taona; ndimo musalandira kumariza kwatu.
12 Ngati dinakuuzani ndi zintu za pansi, ndimo musamvana,
bwanje mudzamvana, ngati dikuuzani ndi zintu za kumwa-
13 mba? Ndimo palibe muntu anakwera kumwamba, koma
iemwe natsika kumwamba, *inde* Mwana wa muntu, iemwe
14 ali m' mwamba. Ndimo monga Moses natukula njoka m'
tshipululu, inde tshointsho Mwana wa muntu akanatuku-
15 lidwa: kuti iemwe amvana angopotshera mwa ie moyo
wosamariza.

16 Kuti Mulungu monga nakonda dziko, kuti napatsa
Mwana watshi wobadwa eka, monga kuti iemwe amvana ndi
ie sakamwazika, koma akapotshera moyo wosamariza.
17 Kuti Mulungu sanatumiza Mwana mwa dziko ku weruza

dziko; koma monga kuti dziko likapulumutsidwa ndi ie.
Iemwe amvana ndi ie wosaweruzidwa iemwe wosamvana 18
waweruzidwa kali, tshifuka sanamvana ndi dzina la Mwana
wa Mulungu wobadwa eka. Ndimo kumene kuli kuweruza, 19
kuti kuunika kunadza m' dziko, ndi antu nakonda ndima kopa-
mbana kuunika; kuti ntshito zao zinali zoipa. Kuti onse 20
omwe atshita mpulupulu akwia ndi kuunika, ndimo osadza
kwa kuunika, kani ntshito zao zikanasulumulidwa. Koma 21
iemwe atshita nteradi adza kwa kuunika, monga kuti ntshito
zatshi zingosonyezedwa, kuti zinatshitidwa mwa Mulungu.

Pambuiu pa zintu zimenezi Yesu nafika ndi akupunzira 22
atshi m' dziko la Yudeya; ndi apo nakala nao, nabapatiza.
Ndimo onso Yohane analikubapatiza mwa Henon pafupi ndi 23
Salem, tshifuka kuti anali madzi ambiri apo: ndimo nafika,
nabapatizidwa. Tshifuka kuti Yohane sanaikidwa tsopano 24
m' nyumba ya ndima. Ndimo kunauka kufunsa mwa 25
akupunzira a Yohane ndi Myuda ndi kusambitsa. Ndimo 26
nafika kwa Yohane, nanena nai', Rabi, iemwe anali ndi iwe
patsidia lidya la Yordan, ku emwe wamariza, ona, iemwe
abapatiza, ndi antu onse adza kwa ie. Yohane naiang'ka 27
nati, Muntu wosadziwa ku landira kantu, kani kapatsidwa
kwa ie kwa kumwamba. Inu noka mumariza ndi ine, kuti 28
dinati, Sindiri Kristu, koma, kuti dinatumizidwa patsogolo
pa ie. Iemwe apotshera tshikwati ali wokwati: koma mbali 29
wa wokwati, emwe aima namva ie, asekera kwambiri tshi-
fuka tsha liu la wokwati: ndimo tshimenetshi tshimwemwe
tshanga tshadzaza. Ie akanakula, koma ine dikanatshepa. 30

Iemwe adzera ku mwamba ali wopambana onse: iemwe 31
ali wapansi ali wapansi, ndimo wa pansi alankula: iemwe
adzera kumwamba ali wopambana onse. Tshomwe watshi- 32
ona ndi watshimva, ndi tshimene atshimariza; ndimo palibe
muntu alandira kumariza kwatshi. Iemwe walandira 33
kumariza kwatshi wasindikiza ndi *tshimene*, kuti Mulungu
ali wanteradi. Kuti iemwe Mulungu watumiza alankula 34
mau a Mulungu: kuti wosapatsa Nzimu ndi muyezo. Atate 35
akonda Mwana, napatsa zintu zonse m' dzanja latshi. Iemwe 36
amvana ndi Mwana ali ndi moyo wosamariza; koma iemwe
wosamvana ndi Mwana sadzaona moyo, koma kukwia kwa
Mulungu kukala pa ie.

Ndimo ntawi Mwini nadziwa bwanje Afarisi anamva kuti 4
Yesu analikupanga ndimo analikubapatiza akupunzira kopa-
mbana Yohane (koma Yesu eka sanabapatiza, koma aku- 2

3 punzira atshi), nasia Yudeya, namuka anso m' Galileya.
4,5 Ndimo akanapita m' Samariya. Ndimo afika ku mzinda wa
Samariya, utshedwa Sikare, pafupi ndi munda womwe
6 Yakobi napatsa ku Yosefe mwana watshi: ndimo kasope
wa Yakobi anali apo. Ndimo Yesu, analema ndi ulendo
watshi, nakala tshointsho pa kasope. Linali pa ora latshisanu
7 ndi tshimodzi. Adza nkazi wa Samariya ku tunga madzi:
8 Yesu anena nai', Patsa ine ku mwa. Kuti akupunzira atshi
9 anang'ka ku mzinda ku gula kudia. Ndimo nkazi wa
Samariya anena nai', Kuli bwanje kuti iwe, uli Myuda,
ufunsa kumwa kwa ine, emwe diri nkazi wa Samariya?
10 (Kuti Ayuda osazolowerana ndi Asamariya). Yesu naiang'ka
nanena nai', Ngati unadziwa mtulu wa Mulungu, ndi iemwe
anena ndi iwe, Patsa ine ku mwa; unganafunsa ie, ndi-
11 mo ie anganakupatsa madzi amoyo. Nkazi anena nai',
Fumu, ulibe tshotungira, ndi tshitsime tshiri tshakuya:
12 ndimo kwa kuti uli ndi madzi amoyo amene? Kodi uli
wang'kuru ndi atatu atu Yakobi, emwe natipatsa tshitsime,
namwa mwa itsho ie eka, ndi ana atshi, ndi ng'ombe zatshi?
13 Yesu naiang'ka nanena nai', Iemwe amwa ndi madzi amene
14 adzamva ludzu unso: koma iemwe amwa ndi madzi omwe
didzapatsa ie sadzamva ludzu ntawi ina; koma madzi omwe
didzampatsa adzakala mwa ie kasope wa madzi kutukula
15 kwa moyo wosamariza. Nkazi anena nai', Fumu, ndipatse
madzi amene, kuti sindimva ludzu, kapena sindidza kuno
16 ku tunga. Yesu anena nai', Muka, itana mamuna wako,
17 nudza kuno. Nkazi naiang'ka nanena nai', Diribe mamuna.
18 Yesu anena nai' Wanena bwino, Diribe mamuna: kuti
unali ndi amuna asanu; ndi iemwe uli nai', tsopano siali
19 mamuna wako: tshimene wanena tshanteradi. Nkazi anena
20 nai', Fumu, didziwitsa kuti uli mprofeti. Atatu atu ana-
pembedza m' piri limene; ndimo munena, kuti m' Yerusa-
21 lem ali malo pomwe antu akanapembedza. Yesu anena nai',
Nkazi, mvana ndi ine, ora lidza, ntawi musadzapembedza
Atatu, kapena m' piri limene, kapena m' Yerusalem.
22 Mupembedza tshomwe musadziwa: tipembedza tshomwe
23 tidziwa: kuti kupulumutsa kuli kwa Ayuda. Koma ora
lidza, ndi tsopano liri, ntawi opembedza oona adzapembedza
Atate ndi nzimu ndi nteradi: kuti atshointshi Atate afuna
24 ku kala opembedza atshi. Mulungu ali Nzimu: ndi omwe
apembedza ie akanapembedza ndi nzimu ndi nteradi.
25 Nkazi anena nai', Didziwa kuti Mesiya adza (iemwe atshe-

dwa Kristu): ntawi anadza, adzauza ife zintu zonse. Yesu 26
anena nai', Ine emwe dilankula ndi iwe diri *ie*.

Ndimo pompo nafika akupunzira atshi; nazizwa kuti 27
analikulankula ndi nkazi; koma palibe muntu nati, Ufuna
tshiani? kapena, Ulankula nai' bwanje? Ndimo nkazi 28
nasia mbia yatshi ya madzi, nang'ka muzinda, ndimo anena
ndi antu, Idzani, onani muntu, emwe anandiuza zintu 29
zonse zomwe dinazitshita *ntawi ina*: kodi amene siali
Kristu? Naturuka muzinda, ndimo analikufika kwa ie. 30
Pa ntawi imene akupunzira napempa ie, kuti, Rabi, idia. 31
Koma nanena nao, Diri ndi kudia ku dia komwe simudziwa. 32
Ndimo akupunzira nafunsana, Kodi muntu modzi wate- 33
ngera ie *kantu* ku dia? Yesu anena nao, Kudia kwanga kuli 34
ku tshita kufuna kwa iemwe ananditumа, ndi ku ta ntshito
yatshi. Kodi simunena, Itsala miezi inai, ndimo masika 35
adza? onani, dinena ndi inu, Tukulani maso anu, ndi
muyang'ane pa minda, kuti iri yoyera tsopano kwa
masika. Iemwe atema alandira kulipira, nasong'kanitsa 36
dzobala kwa moyo wosamariza; kuti iemwe abzala ndi
iemwe atema angosekerana. Kuti mwa itsho uli mwambi 37
woona, Modzi abzala, wina atema. Dinatuma inu ku tema 38
tshomwe pomwe musanatshita: ena nagwira ntshito, ndimo
munaloa m' ntshito zao.

Ndimo kwa mzinda umene ambiri a Asamariya anamvana 39
ndi ie tshifuka tsha mau a nkazi, emwe namariza, Nanena
ndi ine zintu zonse zomwe dinazitshita *ntawi ina*.
Tshointsho ntawi Asamariya anadza kwa ie, namfunsa 40
ku kala ndi awa: nakala apo masiku awiri. Ndi ambiri 41
ena anamvana tshifuka tsha mau atshi; nanena ndi nkazi, 42
Tsopano timvana, si tshifuka tsha kulankula kwako: kuti
tamva kwa ife toka, ndimo tidziwa kuti amene ali nditu
Mpulumutsi wa dziko.

Ndimo pambuiu masiku awiri natshoka apo ku Galileya. 43
Kuti Yesu eka namariza, kuti mprofeti wosapotshera ulemu 44
m' dziko latshi. Ndimo ntawi nafika m' Galileya, Agalileya 45
nalandira ie, anaona zintu zonse zomwe nazitshita m' Yeru-
salem pa kudia: kuti awa anso nang'ka kwa kudia.

Ndimo nafika anso kwa Kana wa Galileya, pomwe ie 46
napanga madzi vinyo. Ndimo kunali wotshuka, mwana wa
emwe anadwala pa Kapernahum. Ntawi anamva kuti Yesu 47
naturuka Yudeya m' Galileya, nang'ka kwa ie, nafunsa *ie*
kuti akatsika, nakatshiritsa mwana watshi; kuti anafuna

48 ku fa. Ndimo Yesu nanena nai', Kani muona zizindikilo
49 ndi zozizwa, musadzamvana. Wotshuka anena nai', Fumu,
50 tsika patsogolo mwana wanga afa. Yesu anena nai', Muka;
mwana wako ali ndi moyo. Muntu namvana mau omwe
51 Yesu ananena nai', namuka. Ndimo tsopano analikutsika,
akapolo atshi nakomana nai', kunena, kuti mwana watshi ali
52 ndi moyo. Ndimo nafunsa awo ora lanje naamba ku
tshira. Ndimo nanena nai', Dzulo pa ora latshisanu ndi
53 tshiwiri malungo namleka. Ndimo atatu *atshi* nadziwa kuti
*tshinali* pa ora lomwe mwa ilo Yesu nanena nai', Mwana
wako ali ndi moyo: ndi ie eka namvana, ndi banja latshi
54 lonse. Tshimene tshiri inso tshizindikilo tshatshiwiri
tshomwe Yesu natshita, anaturuka kwa Yudeya m'
Galileya.

5 Pambuiu zintu zimene kunali kudia kwa Ayuda; ndimo
Yesu nakwera ku Yerusalem.
2 Ndimo kunali m' Yerusalem pa *tshitseko* tsha nkosa
tamanda, lomwe litshedwa m' Tshihebere Betesda, kunali
3 ndi mabalanda asanu. Mwa awo anagona antu ambiri a
5 omwe adwala, a akungu, a opunduka, a ouma. Ndimo
kunali apo muntu modzi, emwe anali ndi kufoka kwatshi
6 dzaka makumi atatu ndi dzisanu ndi dzitatu. Ntawi Yesu
namona kugona, nadziwa kuti anali tsopano ntawi yeitali
7 *tshointsho*, anena nai', Kodi ufuna ku tshiritsidwa? Muntu
wodwala naiang'ka ie, Fumu, diri wopanda muntu, ntawi
madzi abvundukidwa, ku ika ine m' tamanda: koma ntawi
8 dirinkudza, wina atsika patsogolo pa ine. Yesu anena nai',
9 Uka, tukula mpasa yako, nuenda. Ndimo tsopano lino
muntu watshiritsidwa, natukula mpasa yatshi naenda.
10 Ndimo dzua lomwe linali sabata. Ndimo Ayuda nanena
ndi iemwe anatshiritsidwa, Liri dzua la sabata, ndimo
11 sitshamau kwa iwe ku nyamula mpasa yako. Koma
naiang'ka awo, Iemwe wanditshiritsa, iemwe nanena ndi ine,
12 Tukula mpasa yako, nuenda. Namfunsa, Muntu ali ndani
13 iemwe nanena ndi iwe, Tukula *mpasa yako*, nuenda? Koma
iemwe watshiritsidwa sanadziwa anali ani: kuti Yesu ana-
14 tshoka eka, kunali antu ambiri m' malo. Pambuiu Yesu
ampeza m' tempile, nanena nai', Ona, utshiritsidwa: usa-
tshimwa anso, kani tshintu tshoipa tshopambana tshidzafika
15 pa iwe. Muntu namuka, nauza Ayuda kuti anali Yesu
16 iemwe napanga ie wolimba. Ndimo kwa tshifukwa tshimene
Ayuda anazunza Yesu, tshifuka kuti natshita zintu zimenezi

pa sabata. Koma Yesu naiang'ka awo, Atatu anga atshita 17
inde kwa ntawi yatsopano, ndimo ditshita. Ndimo kuti 18
kwa tshifukwa tshimene Ayuda nafuna kopambana kumpa,
tshifuka anaswa si sabata loka, koma anso natsha Mulungu
Atatu atshi, kupanga ie eka modzimodzi ndi Mulungu.
Ndimo Yesu naiang'ka nanena nao, 19
Dinena ndi inu nditu, nditu, Mwana wosadziwa ku tshita
kantu eka, koma tshomwe aona Atate kutshita: kuti zintu
zomwe azitshita, zimenezo Mwana atshita anso modzimodzi.
Kuti Atate akonda Mwana, nasonyeza ie zintu zonse zomwe 20
ie eka atshita: ndimo adzasonyeza ie ntshito zazikuru zopa-
mbana zimenezi, kuti muzizwe. Kuti monga Atate aukitsa 21
akufa nafulumiza awo, inde tshointshi Mwana afulumiza
omwe *ie* afuna. Kuti Atate aweruza palibe muntu, koma 22
wapatsa kuweruza konse kwa Mwana; kuti onse angoleme- 23
keza Mwana, inde monga alemekeza Atate. Iemwe wosale-
mekeza Mwana wosalemekeza Atate emwe anatumiza ie.
Dinena ndi inu nditu, nditu, Iemwe amva mau anga, 24
namvana ndi iemwe anditumiza, ali ndi moyo wosamariza,
ndimo wosafika mwa kuweruza, koma wapita kwa imfa ku
moyo. Dinena ndi inu nditu, nditu, Ora lirinkudza, ndi 25
tsopano liri, ntawi akufa adzamva liu la Mwana wa Mu-
lungu; ndi omwe amva adzakala ndi moyo. Kuti monga 26
Atate ali ndi moyo mwa ie eka, inde tshointsho anapatsa ku
Mwana anso ku potshera moyo mwa ie eka: ndimo napatsa ie 27
mpamvu ku tshita kuweruza, tshifuka kuti ali Mwana wa
muntu. Musazizwa ndi tshimene: kuti ora lirinkudza, mwa 28
lomwe onse omwe ali m' mianda adzamva liu latshi, nadza- 29
turuka; omwe anatshita bwino, kwa kuukirira kwa moyo; ndi
omwe anatshita koipa, kwa kuukirira kwa kuweruza.
Didziwa mwa ine ndeka ku tshita palibe kantu: monga 30
dimva, diweruza: ndimo kuweruza kwanga kuli kodeka;
tshifukakuti difuna si kufuna kwanga, koma kufuna kwa emwe
ananditumiza. Ngati dimariza ndi ine ndeka, kumariza 31
kwanga si kuli kwanteradi. Kuli wina emwe amariza ndi ine; 32
ndimo didziwa kuti kumariza komwe amariza ndi ine kuli
kwanteradi. Munatumiza kwa Yohane, ndimo wamariza ndi 33
nteradi. Koma kumariza komwe dilandira sikuli kwa muntu: 34
koma dinena zintu zimenezi, kuti mungopulumutsidwa.
Anali muni wakuaka ndi wakuwala: ndimo munalikufuna 35
kwa ntawi ku sekera mwa kuunika kwatshi. Koma 36
kumariza komwe diri nako kuli kopambana ndi *komwe kwa*

Yohane: kuti ntshito zomwe Atate wandipatsa kuzita,
ntshito zimenezi zomwe ditshita, zimariza ndi ine, kuti
37 Atate wanditumiza. Ndi Atate emwe ananditumiza, wa-
mariza ndi ine. Kapena musamva liu latshi ntawi ina,
38 kapena musanaona makalidwe atshi. Ndimo musapotshera
mau atshi kukala mwa inu: kuti emwe ie natumiza
39 simumvana nai'. Musaka malemba, kuti mwa awo muganiza
mupotshera moyo wosamariza; ndi amene ali omwe amariza
40 ndi ine; ndimo musafuna ku dza kwa ine, monga kuti
41 mungopotshera moyo. Sindilandira kupambana kwa antu.
42 Koma didziwa inu, kuti musapotshera kukonda kwa
43 Mulungu mwa inu noka. Dadza m' dzina la Atatu anga,
ndimo musalandira ine: ngati wina adzadza m' dzina latshi,
44 ie mudzalandira. Bwanje mudziwa ku mvana, omwe ala-
ndira kupambana modzi kwa wina, ndimo kupambana komwe
45 *kudzera* kwa Mulungu eka musafuna? Musaganiza kuti
didzatshula inu kwa Atate: alipo modzi emwe atshula inu,
46 *inde* Moses, mwa emwe munaika kulingalira kwanu. Kuti
ngati munamvana ndi Moses, mukamvana ndi ine; kuti
47 nalemba ndi ine. Koma ngati musamvana ndi malemba
atshi, bwanje mudzamvana ndi mau anga?

6 Pambuiu zintu zimenezi Yesu namuka ku patsidia lina
la nyanja ya Galileya, yomwe iri *nyanja* ya Tiberiyas.
2 Ndimo antu ambiri namtsata, tshifuka kuti naona zizindikilo
3 zomwe natshita ndi awo omwe anali odwala. Ndimo Yesu na-
4 kwera pa piri, ndimo nakala apo ndi akupunzira atshi. Ndimo
5 mpasika, kudia kwa Ayuda, kunali pafupi. Ndimo Yesu
kutukula maso atshi, ndimo kuona kuti antu ambiri adza
kwa ie, anena ndi Filipu, Kuti tidzagula mikate, kuti amene
6 angodia? Ndimo tshimene nanena ku yesa ie: kuti nadziwa
7 ie eka tshomwe nafuna ku tshita. Filipu naiang'ka ie, Made-
nariyon mazana awiri a mikate osali ambiri ku awa, kuti onse
8 angotenga kang'ono. Modzi wa akupunzira atshi, Andreya,
9 mpwatshi wa Simon Petros, anena nai', Alipo nyamata pano,
iemwe apotshera mikate isanu ya barle, ndi tinsomba tiwiri:
koma zimene zinali bwanje mwa tshuruka tshointsho?
10 Yesu nati, Pangani antu ku kala pansi. Ndimo kunali
maudzu ambiri pa malo. Ndimo antu nakala pansi, m'
11 kutshuruka kunali kwa mazousan asanu. Ndimo Yesu
natenga mikate; ndimo ntawi ananena tshakoma, napatsa
ku awa omwe nakala pansi; ndi tshointsho ndi tinsomba
12 monga ambiri anafuna. Ndimo ntawi anakuta, anena ndi

akupunzira atshi, Song'kani nyenyeswa zotsala, kuti palibe
kantu kamwazike. Ndimo nasong'kanitsa izo, nadzaza 13
mitanga kumi ndi iwiri ndi nyenyeswa za mikate isanu ya
barle, zomwe zinatsala ku awo omwe anadia. Ndimo ntawi 14
antu naona tshizindikilo tshomwe natshita, nati, Amene ali
nditu mprofeti emwe adza m' dziko.

Ndimo Yesu kudziwa kuti afuna ku dza ku tenga ie ndi 15
mpamvu, ku panga ie fumu yotshuka, namuka anso pa
piri ie eka.

Ndimo ntawi madzulo anadza, akupunzira atshi natsika 16
ku nyanja; naloa m' tshombo, nalikuyambuka nyanja ku 17
Kapernahum. Ndimo tsopano kunali ndima, ndimo Yesu
sanafika kosuntira ku awa. Ndimo nyanja inali ku uka 18
tshifuka tsha mpepo yambiri yomwe inaomba. Ndimo 19
ntawi anapalasa mastadia makumi awiri ndi asanu, kapena
makumi atatu, aona Yesu kuenda pa nyanja, ndimo adza
pafupi ndi tshombo: ndimo naopa. Koma anena nao, Diri 20
ine; musaopa. Ndimo nalandira ie ndi kufuna kwao m' 21
tshombo: ndimo nsanga tshombo tshinali kumtunda komwe
analikung'ka.

Pa mawa antu ambiri omwe naima patsidia lina la nyanja 22
naona kuti palibe katshombo kena apo, koma kamodzi, ndi
kuti Yesu sanaloa ndi akupunzira atshi m' tshombo, koma
akupunzira atshi anamuka oka (koma tinadza tidzombo ku 23
Tiberiyas pafupi ndi malo pomwe anadia nkate pambuiu
Mwini ananena tshakoma); ndimo ntawi antu ambiri naona 24
kuti Yesu sanali apo, kapena akupunzira atshi, awa naloa m'
tidzombo, nafika ku Kapernahum, kufuna Yesu. Ndimo 25
ntawi anapeza ie patsidia lina la nyanja, nanena ndi ie,
Rabi, unafika kuno liti? Yesu naiang'ka awo nati, Dinena 26
ndi inu nditu, nditu, Mufuna ine, si tshifuka munaona
zizindikilo, koma tshifuka munadia ndi mikate, munakuta.
Gwirani ntshito si kwa kudia komwe kumwaza, koma kwa 27
kudia komwe kutsala kwa moyo wosamariza, womwe
Mwana wa muntu adzapatsa kwa inu: kuti ie Atate, *inde*
Mulungu, anasindikiza. Ndimo nanena nai', Tikatshita 28
tshiani, kuti tingotshita ntshito za Mulungu? Yesu 29
naiang'ka nanena nao, Imene iri ntshito ya Mulungu, kuti
mumvana ndi ie emwe ie anatumiza. Ndimo nanena nai', 30
Ndimo utshita tshiani kwa tshizindikilo, kuti tingoona,
ndimo timvana ndi iwe? utshita tshiani? Atatu atu anadia 31
mana m' tshipululu; monga alembedwa, Napatsa awo nkate

32 kwa kumwamba ku dia. Ndimo Yesu nanena nao, Dinena
ndi inu nditu, nditu, Sanali Moses emwe napatsa inu nkate
kwa kumwamba; koma Atatu anga apatsa inu nkate woona
33 kwa kumwamba. Kuti nkate wa Mulungu uli umene
womwe utsika kwa kumwamba, ndimo upatsa moyo kwa
34 dziko. Ndimo nanena nai', Mwini, ntawi yonse patsa ife
35 nkate umene. Yesu nanena nao, Diri nkate wa moyo:
iemwe adza kwa ine sadzamva njala, ndi iemwe amvana ndi
36 ine sadzamva ludzu ntawi ina. Koma dinanena ndi inu,
37 kuti mwaona ine, ndimo simumvana. Onse omwe Atate
apatsa ine adzadza kwa ine; ndimo iemwe adza kwa ine
38 sindidzaturutsa nditu. Kuti datsika kumwamba, si ku tshita
kufuna kwanga, koma kufuna kwa emwe ananditumiza.
39 Ndimo kumene kuli kufuna kwa iemwe ananditumiza, kuti
wa onse omwe wapatsa ine sindidzamwaza kantu, koma
40 didzaukitsa pa dzua lomariza. Kuti kumene kuli kufuna
kwa Atatu anga, kuti onse omwe aona Mwana, ndimo
amvana ndi ie, akapotshera moyo wosamariza; ndimo
didzaukitsa ie pa dzua lomariza.

41 Ndimo Ayuda anandandaulira ie, tshifuka anati, Diri nkate
42 womwe unatsika kumwamba. Ndimo anati, Kodi amene
siali Yesu, mwana wa Yosefe, atatu atshi ndi amai atshi a
emwe tidziwa? bwanje tsopano anena, Datsika kwa ku-
43 mwamba? Yesu naiang'ka nanena nao, Musandandaula inu
44 noka. Palibe muntu adziwa ku dza kwa ine, kani Atate
iemwe ananditumiza akoka ie: ndimo didzaukitsa ie m'
45 dzua lomariza. Alembedwa mwa aprofeti, Ndimo onse
adzapunzitsidwa ndi Mulungu. Onse anamva ndi Atate,
46 ndimo anapunzira, adza kwa ine. Si kuti muntu modzi
waona Atate, koma iemwe ali kwa Mulungu, ie waona
47 Atate. Dinena ndi inu nditu, nditu, Iemwe amvana
48,49 apotshera moyo wosamariza. Diri nkate wa moyo. Atatu
50 anu nadia mana m' tshipululu, ndimo anafa. Umene
uli nkate womwe udzera kumwamba, kuti muntu angodia
51 ndi uo, ndimo wosafa. Diri nkate wamoyo womwe
unatsika kumwamba: ngati muntu wina adia wa nkate
umene, adzakala ndi moyo kwa ntawi zonse: inde ndimo
nkate womwe didzapatsa uli nyama yanga, kwa moyo wa
dziko.

52 Ndimo Ayuda natetana iwo oka, kuti, Bwanje muntu
53 amene adziwa kutipatsa nyama yatshi ku dia? Ndimo
Yesu nanena nao, Dinena ndi inu nditu, nditu, Kani mudia

nyama ya Mwana wa muntu ndi ku mwa mwazi watshi,
musapotshera moyo mwa inu. Iemwe adia nyama yanga 54
ndi ku mwa mwazi wanga apotshera moyo wosamariza;
ndimo didzamukitsa pa dzua lomariza. Kuti nyama yanga 55
iri kudia nditu, ndi mwazi wanga uli kumwa nditu. Iemwe 56
adia nyama yanga ndi ku mwa mwazi wanga akala mwa ine,
ndi ine mwa ie. Monga Atate wamoyo ananditumiza, 57
ndimo diri ndi moyo tshifuka tsha Atate; monga iemwe
adia ine, ie enso adzakala ndi moyo tshifuka tsha ine.
Umene uli nkate womwe unatsika kwa kumwamba: si 58
monga atate anadia, ndimo anafa: iemwe adia nkate umene
adzakala ndi moyo ntawi zonse. Zintu zimenezi ananena m' 59
sinagoge, monga napunzitsa m' Kapernahum.

Ndimo ambiri a akupunzira atshi, ntawi anamva, nati, 60
Kumene kuli kunena kolimba; ndani adziwa ku mva?
Koma Yesu kudziwa mwa ie eka kuti akupunzira atshi 61
nandandaula ndi kumene, nanena nao, Kodi kumene kukwi-
itsa inu? *Nanga* ngati mukaona Mwana wa muntu kukwera 62
komwe anali patsogolo? Unali nzimu womwe ufulumiza; 63
nyama yosapindula kantu: mau omwe dalankula ndi inu ali
nzimu, ndimo ali moyo. Koma kuli ena a inu omwe 64
osamvana. Kuti Yesu nadziwa kwa kwiamba omwe anali
omwe osanamvana, ndi emwe adzamzonda. Ndimo nati, 65
Kwa tshifukwa tshimene danena ndi inu, kuti palibe muntu
adziwa ku fika kwa ine, kani tshipatsidwa kwa ie ndi Atate.

Kwa tshimene ambiri a akupunzira atshi nabwera, ndimo 66
sanaenda nai' ntawi ina. Ndimo Yesu nanena ndi kumi 67
ndi awiri, Kodi mufuna anso ku muka? Simon Petros 68
naiang'ka ie, Mwini, kwa emwe tidzang'ka? upotshera mau
a moyo wosamariza. Ndimo tamvana ndimo tidziwa kuti 69
uli Woyera wa Mulungu. Yesu naiang'ka awo, Kodi sindina- 70
sang'ka inu kumi ndi awiri, ndimo modzi wa inu ali diabolos?
Ndimo nanena ndi Yuda *mwana* wa Simon Sikariyoti, kuti 71
kunali ie emwe akamzonda, *kuli* modzi wa kumi ndi awiri.

Ndimo pambuiu zintu zimenezi Yesu naenda m' Galileya: 7
kuti sanafuna ku enda m' Yudeya, tshifuka Ayuda nafuna
kumpa. Ndimo kudia kwa Ayuda, kudia kwa masasa, 2
kunali pafupi. Ndimo abali atshi nanena nai', Tshoka pano, 3
ndimo enda kwa Yudeya, kuti akupunzira ako onso aone
ntshito zako zomwe utshita. Kuti palibe muntu atshita 4
kantu kutseri, ndimo ie eka afuna ku dziwidwa poyera.
Ngati utshita zintu zimenezi, udzisonya kwa dziko. Kuti 5

6 inde abali atshi sanamvana ndi ie. Ndimo Yesu anena nao,
Ntawi yanga siinafika kosuntira; koma ntawi yanu iri
7 yakuta ntawi zonse. Dziko losadziwa kukukwiirani; koma
ndine lirikukwia, tshifuka dimariza ndi ilo, kuti ntshito
8 zatshi ziri zoipa. Kwerani ku kudia: sindikwera kosuntira ku
kudia kumene; tshifuka ntawi yanga siinadzaza kosuntira.
9 Ndimo ntawi ananena nao zintu zimene, nakala m' Galileya.
10 Koma ntawi abali atshi anakwera kwa kudia, pomwe ie
11 enso nakwera, si poyera, koma monga kutseri. Ndimo
12 Ayuda namfuna pa kudia, nati, Alikuti? Ndimo kunali
kundandaula kwambiri ndi ie mwa antu ambiri: ena nati,
Ali muntu wabwino; ena nati, Si tshointsho, koma aso-
13 tsheretsa antu ambiri. Koma palibe muntu nalankula
poyera ndi ie tshifuka naopa Ayuda.
14 Koma ntawi kunali tsopano pakati pa kudia Yesu nakwera
15 kwa tempile, napunzitsa. Ndimo Ayuda nazizwa, kuti,
Muntu amene adziwa malemba bwanje, sanapunzira ntawi
16 ina? Ndimo Yesu naiang'ka awo, nati, Kupunzitsa kwanga
17 si kuli kwanga, koma kwa iemwe ananditumiza. Ngati
muntu modzi afuna ku tshita kufuna kwatshi, adzadziwa
ndi kupunzitsa, kapena kuli kwa Mulungu, kapena dilankula
18 ndeka. Iemwe alankula eka asaka kupambana kwatshi:
koma iemwe asaka kupambana kwa iemwe anamtumiza,
19 iemwe ali wanteradi, ndimo mwa ie mulibe mpulupulu. Kodi
Moses sanakupatsani mau, ndimo palibe modzi wa inu asunga
20 mau? Mufunira anje kundipa? Antu ambiri naiang'ka,
21 Uli ndi demon: afuna kukupa ndani? Yesu naiang'ka
nanena nao, Dinatshita ntshito imodzi, ndimo muzizwa onse.
22 Kwa tshifukwa tshimene Moses wakupatsani kudula (si
tshifuka kuli kwa Moses, koma kwa atate); ndimo pa sa-
23 bata mudula muntu. Ngati muntu alandira kudula pa sabata,
monga kuti mau a Moses asangosweka; kodi mukwia ndi
ine, tshifuka datshiritsa nditu mamuna pa sabata? Musawe-
24 ruza ofana ndi nkope, koma weruzani kuweruza kodeka.
25 Ndimo ená a Akuyerusalem nati, Kodi suyu iemwe afuna
26 kumpa? Ndimo ona, alankula poyera, ndimo anena palibe
kantu ndi ie. Kodi oweruza adziwa nditu kuti amene ali
27 Kristu? Koma tidziwa muntu amene wadzera kuti: koma
ntawi Kristu afika, palibe modzi adziwa adzera kuti.
28 Ndimo Yesu nalira m' tempile, kupunzitsa ndi kuti, Mundi-
dziwa, ndi mudziwa didzera kuti; ndimo sindifika ndeka,
koma iemwe ananditumiza ali woona, emwe musadziwa.

Dimdziwa; tshifuka kuti diri kwa ie, ndimo ananditumiza. 29
Ndimo anafuna kumgwira: ndimo palibe muntu naika 30
dzanja latshi pa ie, tshifuka kuti ora latshi sanafika kosu-
ntira. Koma kwa antu ambiri, ambiri anamvana ndi ie; 31
nati, Ntawi Kristu adzafika, kodi adzatshita zizindikilo
zopambana zidya zomwe muntu amene watshita? Afarisi 32
anamva antu ambiri kunong'ona zintu zimenezi ndi ie;
ndimo adzukuru akuru ndi Afarisi natumiza adindo ku-
mgwira. Ndimo Yesu nati, Ntawi yeing'ono yatsala diri 33
ndi inu, ndimo ding'ka kwa emwe ananditumiza. Mudza- 34
ndifuna, ndimo musadzandipeza: ndimo komwe diri, musa-
dziwa ku fika. Ndimo Ayuda nauzana, Muntu amene 35
adzang'ka kuti, pomwe sitidzampeza? kodi adzang'ka kwa
Kubalalika mwa Agrike, napunzitsa Agrike? Mau amene 36
ali tshiani omwe nanena, mudzandifuna, ndimo musadzandi-
peza: ndimo komwe diri, musadziwa ku fika?

Ndimo pa dzua lomariza, *dzua* lalikuru la kudia, Yesu 37
naima napfula, kuti, Ngati alipo muntu modzi ali ndi ludzu,
adze kwa ine, namwa. Iemwe amvana ndi ine, monga 38
lemba lati, mitsinje ya madzi amoyo idzaturuka m' mimba
mwatshi. Koma tshimene nanena ndi Nzimu, womwe awo 39
omwe anamvana ndi ie anali ku landira: tshifuka kuti
Nzimu suna*patsidwa* kosuntira; tshifuka Yesu sanapa-
mbanitsidwa kosuntira. Ndimo *ena* a antu ambiri, ntawi 40
anamva mau amene, nati, Amene ali mprofeti nditu. Ena 41
nati, Amene ali Kristu. Koma ena nati, Kodi Kristu adza-
turuka ku Galileya? Kodi lemba silinanena kuti Kristu 42
afika wa mbeu ya Davide, ndimo ku Betelehem, mudzi pomwe
Davide anali? Ndimo kunali kugawa kwa antu ambiri 43
tshifuka tsha ie. Ndimo ena a awo nafuna kumgwira; 44
koma palibe muntu naika manja pa ie.

Ndimo adindo nafika kwa adzukuru akuru ndi Afarisi; 45
nanena nao, Muleka lanje kumtenga? Adindo naiang'ka, 46
Palibe ntawi muntu nalankula tshointsho. Ndimo Afarisi 47
naiang'ka awo, Kodi munasotsheretsedwa anso? Kodi alipo 48
wina wa akuru, kapena wa Afarisi amvana nai'? Koma 49
antu ambiri amene omwe osadziwa mau alumbiridwa. Ni- 50
kodemo anena nao (emwe nafika kwa ie patsogolo, kuli
modzi wa awo), Kodi mau atu aweruza muntu, kani patsogolo 51
amva kwa ie ndimo kudziwa tshomwe atshitshita?
Naiang'ka nanena nai', Kodi uli inso wa Galileya? Saka, 52
ndimo nuona kuti ku Galileya wosauka mprofeti.

53 [Ndimo antu onse nang'ka ku nyumba zao: koma Yesu
8 nang'ka ku piri la Maolive. Ndimo mamawa nafika anso m'
tempile, ndimo antu onse nadza kwa ie; ndimo nakala
3 pansi, napunzitsa awo. Ndimo akulembera ndi Afarisi
atenga nkazi napezedwa ndi tshigololo; namwika pakati,
4 anena nai', Mpunzitsi, nkazi amene wapezedwa alikutshita
5 tshigololo nditu. Ndimo m' mau Moses natiuza ku ponya
6 miala pa otere: ndimo unena tshiani ndi ie? Ndimo
nanena tshimene, kumyesa, kuti anangopotshera *kantu* ku
tshula ie. Koma Yesu nawerama, ndimo ndi tshala tshatshi
7 nalemba pansipo. Koma ntawi anamfunsabe, nadziuka,
nanena nao, Iemwe wa inu, ali wopanda mpulupulu, leka ie
8 kuiamba ku ponya mwala pa ie. Ndimo onso nawerama,
9 ndimo ndi tshala tshatshi nalemba pansi. Ndimo awo,
ntawi anamva, anaturuka kamodzi kamodzi, kuiamba ndi
wang'kuru, *inde* kwa wakutungo: ndimo Yesu anatsala eka,
10 ndi nkazi, pomwe anali, pakati. Ndimo Yesu nadziuka,
nanena nai', Nkazi, ali kuti? Kodi palibe muntu naku-
11 sutsa? Ndimo nati, Palibe muntu, Mwini. Ndimo Yesu
nati, Kapena ine sindikusutsa: muka; kwa tsopano mpulu-
pulu usatshita anso.]

12 Ndimo Yesu nalankula anso nao, kuti, Diri kuunika kwa
dziko: iemwe anditsata sadzapita mudima, koma adzapo-
13 tshera kuunika kwa moyo. Ndimo Afarisi nanena nai',
Umariza ndi iwe eka; kumariza kwako sikuli kwanteradi.
14 Yesu naiang'ka nanena nao, Inde ngati dimariza ine ndeka,
kumariza kwanga kuli kwanteradi; tshifuka didziwa dadzera
kuti, ndi komwe dimuka; koma simudziwa komwe dadzera,
15 ndi komwe dimuka. Muweruza kofana ndi nyama; di-
16 weruza palibe muntu. Inde ndimo ngati diweruza, kuwe-
ruza kwanga kuli kwanteradi; tshifuka sindiri ndeka, koma
17 Ine ndi Atate emwe ananditumiza. Inde ndimo kule-
mbedwa m' mau anu, kuti kumariza kwa antu awiri kuli
18 kwanteradi. Diri iemwe kumariza ndi ine ndeka, ndimo
19 Atate emwe ananditumiza amariza ndi ine. Ndimo nanena
nai', Atatu ako ali kuti? Yesu naiang'ka, Musadziwa
kapena ine, kapena Atatu anga: ngati munandidziwa,
20 mukadziwa Atatu anga anso. Mau amene nalankula m'
nyumba yolemera, monga napunzitsa m' tempile: ndimo

palibe muntu namgwira; tshifuka ora latshi lisanafika
kosuntira.

Ndimo nanena nao onso, Dimuka, ndimo mudzafuna ine, 21
ndimo mudzafa m' mpulupulu yanu: komwe ding'ka,
musadziwa ku fika. Ndimo Ayuda nati, Kodi adzipa eka, 22
tshifuka ati, Komwe ding'ka, musadziwa ku fika? Ndimo 23
nanena nao, Muli kwa pansi; diri kwa mwamba: muli a
dziko limene; sindiri wa dziko limene. Ndimo dinanena 24
ndi inu, kuti mudzafa m' mpulupulu zanu: kuti kani mu-
mvana kuti diri *ie*, mudzafa m' mpulupulu zanu. Ndimo 25
nanena nai', Uli ani? Yesu nanena nao, Inde modzimodzi
dakulankulani inso kwa kuamba. Dipotshera zintu zambiri 26
ku lankula ndi ku weruza ndi inu: koma iemwe ananditu-
miza ali wanteradi; ndimo zintu zomwe dinamva kwa ie,
zimenezi dilankula m' dziko. Sanadziwa kuti nanena nao 27
ndi Atate. Ndimo Yesu nanena, Ntawi munatukula Mwana 28
wa muntu, pomwe mudzadziwa kuti diri *ie*. Ndimo *kuti*
ditshita palibe kantu ine ndeka, koma monga Atate anandi-
punzitsa, dilankula zintu zimenezi. Ndimo iemwe anandi- 29
tumiza ali ndi ine; sanandileka ndeka; kuti ntawi yonse
ditshita zintu zomwe zisekeretsa ie. Monga nalankula zintu 30
zimenezi, ambiri anamvana ndi ie.

Ndimo Yesu nanena ndi Ayuda omwe anamvana ndi ie, 31
Ngati mukala m' mau anga, muli akupunzira anga nditu;
ndimo mudzadziwa nteradi, ndimo nteradi udzapanga inu 32
aufulu. Naiang'ka ie, Tiri mbeu ya Abraham, ndimo 33
palibe ntawi kosuntira tinali m' ukapolo ku muntu modzi:
unena bwanje, mudzapangidwa aufulu? Yesu naiang'ka awo, 34
Dinena ndi inu nditu, nditu, Iemwe atshita mpulupulu ali
kapolo wa mpulupulu. Ndimo kapolo wosakala m' nyumba 35
ntawi yonse: mwana akala ntawi yonse. Ndimo ngati Mwana 36
akupangani aufulu, mudzakala aufulu nditu. Didziwa kuti 37
muli mbeu ya Abraham; koma mufuna kundipa, tshifuka
mau anga alibe malo mwa inu. Dilankula zintu zomwe 38
daona ndi Atatu *anga*: ndimo inu unso mutshita zintu
zomwe munamva ndi atatu *anu*. Naiang'ka nanena nai', 39
Atatu atu ali Abraham. Yesu anena nao, Ngati munali
ana a Abraham, mukatshita ntshito za Abraham. Koma 40
tsopano mufuna kundipa, muntu emwe wauza inu nteradi;
womwe damva kwa Mulungu: tshimene Abraham sana-
tshitshita. Mutshita ntshito za atatu anu. Nanena nai', 41
Sitinabadwa a tshigololo; tiri ndi Atate modzi, *inde*

42 Mulungu. Yesu nanena nao, Ngati Mulungu anali Atatu
anu, mukakonda ine: kuti dinaturuka ndimo dadzera kwa
Mulungu; kuti kapena sindafika ndeka, koma ie ananditu-
43 miza. Musadziwa kulankula kwanga bwanje? *Inde* tshifuka
44 musadziwa ku mva mau anga. Muli a atatu *anu* diabolos,
ndimo zofuna za atatu anu kuli kufuna kwanu ku tshita.
Ie anali wambanda kwa kuamba, ndimo sanaima m' nteradi,
tshifuka mulibe nteradi mwa ie. Ntawi anena bodza, anena
wa mwini watshi: kuti ali wabodza, ndi atate wa ilo.
45 Koma tshifuka dinena nteradi, musamvana ndi ine.
46 Ndani wa inu asutsa ine ndi mpulupulu? Ngati dinena
47 nteradi, muleka lanje ku mvana ndi ine? Iemwe ali wa
Mulungu amva mau a Mulungu: kwa tshifukwa tshimene
48 simumvana *awo*, tshifuka musali a Mulungu. Ayuda naiang'-
ka nanena nai', Kodi sitinena bwino kuti uli Msamariya,
49 ndimo uli ndi demon? Yesu naiang'ka, Sindipotshera
demon; koma dilemekeza Atatu anga, ndimo musandileme-
50 keza. Koma sindifuna kupambana kwanga: alipo modzi
51 iemwe afuna naweruza. Dinena ndi inu nditu, nditu, Ngati
muntu modzi asunga mau anga, ntawi ina sadzaona imfa.
52 Ayuda anena nai', Tsopano tidziwa kuti uli ndi demon.
Abraham wafa, ndi aprofeti; ndimo uti, Ngati muntu
53 asunga mau anga, ntawi ina sadzalawa imfa. Kodi uli
wang'kuru ndi Abraham atatu atu, emwe wafa? ndimo
54 aprofeti nafa: udzipanga ndani? Yesu naiang'ka, Ngati
didzipambanitsa, kupambana kwanga kuli tshabe: kuli
Atatu anga emwe andipambanitsa; wa iemwe munena, kuti
55 ali Mulungu wanu; ndimo musanamdziwa: koma dimdzi-
wa; ndimo ngati dikanena, sindimdziwa, didzakala wabodza
wofana ndi inu: koma dimdziwa, ndisunga mau atshi.
56 Atatu anu Abraham nakondwera ku ona siku langa; ndimo
57 naliona, nasekera. Ndimo Ayuda nanena nai', Usabadwa
kosuntira dzaka makumi asanu, ndimo waona Abraham?
58 Yesu nanena nao, Dinena ndi inu nditu, nditu, Patsogolo
59 Abraham anakala ine ndiri. Ndimo natola miala ku
ponya ie: koma Yesu nabisala eka, ndimo naturuka m'
tempile.

9 Ndimo monga analikupita, naona muntu emwe anali ndi
2 kungu kwa kubadwa kwatshi. Ndimo akupunzira atshi
namfunsa, kuti, Rabi, watshimwa ndani, muntu amene,
kapena atatu atshi ndi amai atshi, kuti anabadwa wakungu?
3 Yesu naiang'ka, Kapena si muntu amene, kapena si atatu

atshi ndi amai atshi anatshimwa: koma kuti ntshito za
Mulungu zikasonyezedwa mwa ie. Tikanagwira ntshito za 4
emwe ananditumiza, ntawi ya dzua: usiku udza, ntawi
palibe muntu adziwa ku tshita. Ntawi diri m' dziko, diri 5
kuunika kwa dziko. Ntawi ananena tshointsho, nalabvula 6
mate pansi, naomba dote ndi mate, napaka maso atshi ndi
dote, nanena nai', Muka, samba m' tawali la Silowam 7
(lomwe liri lisandukidwa, Kutumidwa). Ndimo namuka,
nasamba, nabwera kuona. Ndimo oiandikila, ndi omwe 8
anamona patsogolo, kuti anali wopempa, nanena, Kodi si
amene emwe nakala napempa? Ena nati, Ali ie: ena nati, 9
Iai, koma ali wofana nai'. Ie nati, Diri *ie*. Ndimo nanena 10
nai', Nanga maso ako anatsegulidwa bwanje? Naiang'ka, 11
Muntu emwe atshedwa Yesu naomba dote, napaka maso
anga, nandiuza, Muka ku Silowam, nusamba: ndimo
dinamuka, dinasamba, dinaona. Ndimo nanena nai', Ali 12
kuti? Anena, Sindidziwa.

Atenga kwa Afarisi iemwe anali ndi kungu kali. 13
Ndimo linali sabata pa dzua lomwe Yesu naomba dote, 14
natsegula maso atshi. Ndimo onso Afarisi inso namfunsa 15
bwanje analandira kuona kwatshi. Ndimo nanena nao,
Naika dote pa maso anga, ndimo dinasamba, ndiona.
Ndimo ena a Afarisi nati, Muntu amene wosali 16
kwa Mulungu, tshifuka wosasunga sabata. Koma ena
nati, Muntu emwe ali wampulupulu adziwa ku tshita
zizindikilo zimenezi bwanje? Ndimo kunali kugawa
mwa awo. Ndimo anena anso ndi muntu wakungu, 17
Unena tshiani ndi ie, m' tshimene kuti anatsegula maso
ako? Ndimo nati, Ali mprofeti. Ndimo Ayuda sana- 18
mvana ndi ie, kuti anali wakungu, ndimo analandira kuona
kwatshi, kwa ntawi anaitana atatu atshi ndi amai atshi a
emwe analandira kuona kwatshi, ndimo nafunsa awo, kuti, 19
Kodi amene ali mwana wanu, iemwe munena wabadwa wa-
kungu? ndimo tsopano aona bwanje? Atatu atshi ndi amai 20
atshi naiang'ka nati, Tidziwa kuti amene ali mwana watu,
ndi kuti anabadwa wakungu: koma tsopano aona bwanje, 21
sitidziwa; kapena ndani anatsegula maso atshi, sitidziwa:
funsani ie; ali mkuru; adzalankula kwa ie eka. Atatu 22
atshi ndi amai atshi nanena zintu zimenezi, tshifuka naopa
Ayuda: kuti Ayuda nabvomerezana kali, kuti ngati muntu
modzi akabvomera kuti *anali* Kristu, akaturutsidwa m'
sinagoge. Ndimo atatu atshi ndi amai atshi nanena, Ali 23

24 mkuru; funsani ie. Ndimo naitana kawiri muntu emwe
anali ndi kungu, nanena nai', Patsa kupambana ku
Mulungu: tidziwa kuti muntu amene ali wampulupulu.
25 Ndimo naiang'ka, Ngati ie ali wampulupulu, sindidziwa:
tshintu tshimodzi didziwa, kuti, dinali wakungu, tsopano
26 diona. Ndimo ananena nai', Natshita tshiani ndi iwe?
27 natsegula maso ako bwanje? Naiang'ka awo, Dakuuzani inde
tsopano, ndimo musanamva: mufuna anso ku mva bwanje?
28 kodi mufuna ku kala akupunzira atshi inso? Ndimo
namnyoza, nati, Uli wakupunzira watshi; koma tiri aku-
29 punzira a Moses. Tidziwa kuti Mulungu walankula ndi
30 Moses: koma muntu amene, sitidziwa adzera kuti. Muntu
naiang'ka nanena nao, Mwa tshimene tshiri tshozizwa, kuti
simudziwa adzera kuti, ndimo anatsegula maso anga.
31 Tidziwa kuti Mulungu wosamva ampulupulu: koma ngati
muntu modzi akala wopembedza wa Mulungu, natshita
32 kufuna kwatshi, amva ie. Kwa kuamba kwa dziko
sitshinamvedwa kuti modzi anatsegula maso a muntu
33 wobadwa wakungu. Ngati muntu amene sanali kwa
34 Mulungu, sanadziwa ku tshita kantu. Anaiang'ka nanena
nai', Wabadwa m' zakwaipa nditu, ndimo kodi utipunzitsa?
Ndimo anamturutsa.

35 Yesu anamva kuti anamturutsa; ndimo kumpeza, nati,
36 Kodi umvana ndi Mwana wa Mulungu? Naiang'ka nati,
37 Ndimo ie ali ndani, Mwini, kuti dingomvana ndi ie? Yesu
nanena nai', Wamona, ndimo emwe alankula ndi iwe ali ie.
38 Ndimo nati, Mwini, dimvana. Ndimo nalemekeza ie.
39 Ndimo Yesu nati, Kwa kuweruza dafika m' dziko limene,
kuti omwe osaona angoona; ndi omwe aona angokala
40 akungu. Amenewo a Afarisi omwe anali nai' namva zintu
41 zimenezi, nanena nai', Kodi tiri akungu unso? Yesu
nanena nao, Ngati muli akungu, mulibe mpulupulu: koma
tsopano munena, Tiona: mpulupulu zanu zikala.

10 Dinena ndi inu nditu, nditu, Emwe wosaloa pa komo m'
tanga la nkosa, koma akwera pa njira ina, amene ali woba
2 ndi wolanda. Koma emwe aloa pa komo ali mbusa wa
3 nkosa. Ku ie tsatshipata atsegula; ndimo nkosa zimva liu
latshi: ndimo aitana nkosa zatshi ndi maina ao, natsogoza
4 izo kunja. Ntawi anaturutsa zatshi zonse, apita patsogolo
pa izo, ndimo nkosa zimtsata: tshifuka zidziwa liu latshi.
5 Koma mlendo zisadzatsata, koma zidzatawa kwa ie:
6 tshifuka zosadziwa liu la alendo. Fanizo limene Yesu

nanena nao; koma sanadziwa ziani zintu zinali zomwe
nalankula nao.
Ndimo Yesu nanena nao onso, Dinena ndi inu nditu, 7
nditu, diri tshitseko tsha nkosa. Onse omwe nafika patso- 8
golo pa ine ali akuba ndi akulanda: koma nkosa sizinamva
awo. Diri tshitseko: ndi ine ngati muntu modzi aloa, 9
adzapulumutsidwa, nadzaloa nadzaturuka, nadzapeza busa.
Woba wosafika, kani kuti abe, ndi ape, ndi amwaze: 10
dinafika kuti angopotshera moyo, ndimo angopotshera *iwo*
kwambiri. Diri mbusa wabwino: mbusa wabwino aika 11
pansi moyo watshi kwa nkosa. Iemwe ali wolipidwa, ndimo 12
wosali mbusa, emwe si mwini watshi wa nkosa, aona
tshirombo tshirikufika, naleka nkosa, natawa, ndimo
tshirombo atshikwatula izo natshibalalitsa *izo: atawa* tshi- 13
fuka ali wolipidwa, ndimo wosasungira nkosa. Diri mbusa 14
wabwino; ndidziwa zanga, ndimo zanga zidziwa ine, inde 15
monga Atate andidziwa, ndimo didziwa Atate; ndimo diika
pansi moyo wanga kwa nkosa. Ndimo nkosa zina dipotshera, 16
zomwe zosali za tanga limene: izo onso dikanatenga, ndimo
zidzamva liu langa; ndimo zidzakala gulu limodzi, mbusa
modzi. Ndimo Atate andikonda, tshifuka diika pansi moyo 17
wanga, monga kuti dingotenga anso. Palibe modzi autshotsa 18
kwa ine, koma diuika pansi ine ndeka. Diri ndi mpamvu
kuuika pansi, ndimo diri ndi mpamvu kuutenga anso. Mau
amene dalandira kwa Atatu anga.
Kunali inso kugawa mwa Ayuda tshifuka tsha mau amene. 19
Ndimo ambiri a awo nati, Ali ndi demon, ndimo ali ndi 20
misala; mumva ie bwanje? Ena nati, Amene osali mau a 21
modzi emwe agwidwa ndi demon. Kodi demon adziwa ku
tsegula maso a akungu?
Ndimo kunali kudia kwa kusonyeza kwa Yerusalem: anali 22
malimwe; ndimo Yesu analikuendaenda m' tempile m' 23
balanda la Solomon. Ndimo Ayuda nazunguniza ie, 24
nanena nai', Ntawi ingati utipanga ku ganizaganiza? Ngati
uli Kristu, utiuze koona. Yesu naiang'ka awo, Dakuuzani, 25
ndimo simumvana: ntshito zomwe ditshita m' dzina la Atatu
anga, zimene zimariza ndi ine. Koma simumvana, tshifuka 26
simuli a nkosa zanga. Nkosa zanga zimva liu langa, ndimo 27
didziwa izo, ndimo zinditsata: ndimo dipatsa izo moyo 28
wosamariza; ndimo sizidzamwazika ntawi ina, ndimo kulibe
modzi adzakwatula izo m' dzanja langa. Atatu anga, emwe 29
wandipatsa *izo*, ali wang'kuru ndi onse; ndimo kulibe modzi

30 adziwa ku kwatula *izo* kwa dzanja la Atate. Ine ndi Atate
31,32 tiri amodzi. Ayuda natola miala anso ku ponya ie. Yesu
naiang'ka awo, Ntshito zabwino zambiri dakuonetsani kwa
Atate; kwa ntshito iti za zimenezo mufuna kundiponya
33 miala? Ayuda naiang'ka ie, Kwa ntshito yabwino sitiku-
ponya miala, koma kwa kutukwana; ndimo tshifuka kuti
34 iwe, uli muntu, udzipanga Mulungu. Yesu naiang'ka awo,
Kodi sikulembedwa m' mau anu, Dinati, Muli milungu?
35 Ngati natsha awo milungu, kwa omwe mau a Mulungu
36 nafika (ndimo mlemba losadziwa ku swedwa), kodi munena
ndi ie, emwe Atate anayeretsa natumiza m' dziko, Utukwa-
37 na; tshifuka dinanena, Diri Mwana wa Mulungu? Ngati
38 sinditshita ntshito za Atatu anga, musandimvana. Koma
ngati dizitshita, inde ngati simumvana ndi ine, mvanani
ndi ntshito: kuti mungodziwa ndi kudziwitsa kuti Atate
39 ali mwa ine, ndi ine mwa Atate. Nafuna anso kumgwira:
ndimo naturuka mwa dzanja lao.

40 Ndimo namuka anso patsidia lina la Yordan ku malo
pomwe Yohane analikubapatiza pa kuamba; ndimo nakala
41 apo. Ndimo ambiri nadza kwa ie; nati, Yohane nditu
natshita palibe tshizindikilo: koma zintu zonse zomwe
42 Yohane nanena ndi muntu amene zinali zanteradi. Ndimo
ambiri namvana ndi ie apo.

11 Ndimo muntu modzi anadwala, Lazaro wa Betaniya, wa
2 mudzi wa Mariya ndi Marta njiratshi. Ndimo anali Mariya
amene emwe anadzosa Mwini ndi mafuta, napukuta mapazi
3 atshi ndi tsisi latshi, mlongwatshi Lazaro nadwala. Ndimo
alongo atshi natumiza kwa ie, kuti, Mwini, ona, iemwe
4 ukonda alikudwala. Koma ntawi Yesu anamva, nati,
Kudwala kumene sikuli kwa kufa, koma kwa kupambana
kwa Mulungu, kuti ndi kumene Mwana wa Mulungu
5 angopambanitsidwa. Ndimo Yesu nakonda Marta, ndi
6 mpwatshi, ndi Lazaro. Ndimo ntawi anamva kuti ie ana-
dwala, nakala pa ntawi imene masiku awiri pa malo pomwe
7 anali. Ndimo pambuiu amene anena ndi akupunzira, Tiende
8 enso ku Yudeya. Akupunzira anena nai', Rabi, Ayuda
tsopano analikufuna ku ponya miala pa iwe; ndimo onso
9 uenda uko? Yesu naiang'ka, Kodi sialipo maora kumi ndi
awiri m' siku *limodzi?* Ngati muntu aendaenda m' dzua,
wosakumudwa, tshifuka aona kuunika kwa dziko limene.
10 Koma ngati muntu aendaenda usiku, akumudwa, tshifuka
11 kuunika kusali mu ie. Nanena zintu zimenezi: ndimo

pambuiu tshimene anena nao, Mbali watu Lazaro wagona;
koma ding'ka, kuti dimukitsa kwa tulo tatshi. Ndimo 12
akupunzira nanena nai', Mwini, ngati wagona, adzapulumu-
tsidwa. Ndimo Yesu ananena ndi imfa yatshi: koma 13
naganiza kuti nanena ndi kupuma ndi tulo. Ndimo Yesu 14
nanena nao koona, Lazaro anafa. Ndimo disekera kwa inu 15
kuti sindinali apo, monga kuti mungomvana; koma tipite
kwa ie. Ndimo Tomas, emwe atshedwa Didimo, nanena 16
ndi akupunzira anzatshi, Tipite enso, kuti tingofa ndi ie.

Ndimo ntawi Yesu nafika, napeza kuti anali m' mwanda 17
tsopano masiku anai. Ndimo Betaniya unali pafupi ndi 18
Yerusalem, pa mastadia kumi ndi asanu; ndimo ambiri a 19
Ayuda nadza kwa Marta ndi Mariya, ku sangalatsa awo pa
mlongo wao. Ndimo Marta, ntawi anamva kuti Yesu ana- 20
linkudza, namuka nakomana nai': koma Mariya nakala m'
nyumba. Ndimo Marta nanena ndi Yesu, Mwini, ngati 21
unali pano, mlongo wanga sakanafa. Ndimo inde tsopano 22
didziwa kuti, tshomwe udzafunsa kwa Mulungu, Mulungu
adzapatsa iwe. Yesu anena nai', Mlongwako adzauka 23
anso. Marta anena nai', Didziwa kuti adzauka anso m' 24
kuukirira pa dzua lomariza. Yesu nanena nai', Diri kuuki- 25
rira, ndi moyo: iemwe amvana ndi ine, ngati afa, inde
adzakala ndi moyo: ndi emwe akala ndi moyo namvana ndi 26
ine palibe ntawi adzafa. Umvana tshimene? Anena ndi 27
ie, Inde, Mwini: damvana kuti uli Kristu, Mwana wa Mulu-
ngu, *inde* iemwe adzadza m' dziko. Ndimo ntawi ananena 28
tshointshi, namuka, naitana Mariya mpwatshi kutseri, kuti,
Mpunzitsi wafika, naitana iwe. Ndimo ie, ntawi anamva 29
tshimene, nauka nsanga, namuka kwa ie. (Ndimo Yesu 30
tsopano sanaloa m' mudzi, koma anali pa malo pomwe Marta
nakomana nai'.) Ndimo Ayuda omwe anali ndi ie m' nyu- 31
mba, ndimo analikusangalatsa ie, ntawi naona Mariya, kuti
nauka nsanga naturuka, namtsata, kuganiza kuti analikuenda
ku mwanda ku lira nsozi apo. Ndimo Mariya, ntawi nafika 32
pomwe Yesu anali, namona, nagwa pa mapazi atshi, kunena ndi
ie, Mwini, ngati unali pano, mlongo wanga sakanafa. Ndi- 33
mo ntawi Yesu naona ie kulira, ndi Ayuda *anso* kulira omwe
nadza nai', nabulira muzimu, nantentemera, nati, Muna-
mwika kuti? Anena nai', Mwini, idza uone. Yesu nalira 34, 35
nsozi. Ndimo Ayuda nanena, Ona bwanje nakonda ie! 36
Koma ena a awo nati, Kodi muntu amene, emwe natsegula 37
maso a emwe anali wakungu, sanadziwa ku panga kuti

38 muntu amene enso sakanafa? Ndimo Yesu kubulira anso
mwa ie eka adza ku mwanda. Ndimo unali panga, ndi
39 mwala unaikidwa pa iwo. Yesu ati, Tshotsani mwala.
Marta, mlongwatshi wa emwe anafa, anena ndi ie, Mwini,
40 tsopano wabvunda: kuti ana*fa* masiku anai. Yesu anena
nai', Kodi sindanena ndi iwe, kuti, ngati umvana, ukaona
41 kupambana kwa Mulungu? Ndimo natshotsa mwala.
Ndimo Yesu natukula maso atshi, nati, Atate, diamika iwe
42 kuti unamva ine. Ndimo dinadziwa kuti umva ine ntawi
zonse: koma tshifuka tsha antu ambiri omwe aima kozu-
ngulira dinatshinena, kuti angomvana kuti wanditumiza.
43 Ndimo ntawi ananena zimenezi, napfula ndi liu lalikuru,
44 Lazaro, turuka. Iemwe anafa naturuka, wamangidwa
dzanja ndi pazi ndi nsaru za mwanda; ndi nkope yatshi
yazungunidwa ndi mrenzo. Yesu anena nao, Masulani ie,
ndimo lekani ie ku ng'ka.
45 Ndimo ambiri a Ayuda, omwe nadza kwa Mariya ndimo
46 anaona tshintu tshomwe natshita, namvana nai'. Koma ena
a awo namuka kwa Afarisi, nauza awo zintu zomwe Yesu
anatshita.
47 Ndimo adzukuru akuru ndi Afarisi nasong'kanitsa gulu
la ankoswe, nati, Titshita tshiani? kuti muntu 'amene
48 atshita zizindikilo zambiri. Ngati tileka ie tshointsho, antu
onse adzamvana ndi ie: ndi Aroma adzadza nadzatshotsa
49 malo atu ndi mtundu watu. Koma modzi wa awo, Kayafa,
kuli ndzukuru wang'kuru tshaka tshimene, nanena nao,
50 Simudziwa kantu konse, kapena simuganiza kuti tshiri
tshabwino kwa inu kuti muntu modzi akafera antu, ndimo
51 kuti mtundu wonse wosakamwazika. Ndimo tshimene sana-
nena ie eka: koma kuli ndzukuru wang'kuru tshaka
52 tshimene, naambirira kuti Yesu akafera mtundu; ndimo si
kwa mtundu woka, koma kuti inso anangosong'kanitsa pa
53 modzi ana a Mulungu omwe abalalika. Ndimo kwa siku
limene nagazitsana monga kuti anangompa.
54 Ndimo Yesu sanaendaenda anso poyera mwa Ayuda,
koma namuka uko ku dziko pafupi ndi tshipululu, muzinda
utshedwa Frayim; ndimo apo nakala ndi akupunzira.
55 Ndimo mpasika wa Ayuda unali pafupi: ndi ambiri na-
kwera ku Yerusalem mwa dziko patsogolo mpasika, ku
56 sambitsa iwo oka. Ndimo nafuna Yesu, nauzana, monga
naima m' tempile, Muganiza anje? Kuti sadzafika ku
57 kudia? Ndimo adzukuru akuru ndi Afarisi anauza mau.

kuti, ngati muntu modzi nadziwa pomwe anali, akasonyeza,
monga kuti anangomgwira.

Ndimo Yesu masiku asanu ndi limodzi patsogolo mpasika 12
nafika ku Betaniya, pomwe anali Lazaro, iemwe Yesu
naukitsa kwa akufa. Ndimo apo napanga ngonero kwa ie: 2
ndimo Marta naimirira; koma Lazaro anali modzi wa awo
omwe nakala pa kudia nai'. Ndimo Mariya natenga poundi 3
la mafuta a nardo, ntengo watshi wapatali wambiri, na-
dzosa mapazi a Yesu, napukuta mapazi atshi ndi tsisi latshi:
ndimo nyumba inadzazidwa ndi kunung'kira kwa mafuta.
Koma Yuda Sikariyoti, modzi wa akupunzira atshi, emwe 4
akamzonda, ati, Mafuta amene sanagulitsidwa bwanje kwa 5
madenariyon mazana atatu, napatsidwa kwa osauka?
Ndimo nanena tshimene, si tshifuka nasungira osauka; 6
koma tshifuka anali woba, ndimo kunali ndi tumba, nanya-
mula zomwe zinaikwa umo. Ndimo Yesu nati, Reka ie 7
kwasunga pa siku la kundiika m' mwanda. Kuti osauka 8
mupotshera ntawi yonse ndi inu; koma ine musapotshera
ntawi yonse.

Ndimo antu atshabe a Ayuda anapunzira anali apo: 9
ndimo nafika, si kwa Yesu eka, koma kuti aone Lazaro onso,
emwe anaukitsa kwa akufa. Koma adzukuru akuru naga- 10
zitsana bwanje angopa Lazaro onso; tshifuka ndi ie Ayuda 11
ambiri namuka, namvana ndi Yesu.

Ndimo mawa antu ambiri omwe anafika kwa kudia, ntawi 12
anamva kuti Yesu analinkudza ku Yerusalem, natenga 13
makwata a kanjedza, naturuka ku komana nai', napfula,
Hosana: Wodala *ali* iemwe afika m' dzina la Mwini, inde
Fumu Yotshuka ya Sirayeli. Ndimo Yesu, ntawi anapeza 14
kaburu, nakala pa iko; monga alembedwa, Musaopa, 15
mwana wankazi wa Ziyon: ona, Fumu Yotshuka yako
ifika, kukala pa mwana wa buru. Zintu zimenezi paku- 16
amba akupunzira atshi sanadziwa: koma ntawi Yesu anapa-
mbanitsidwa, pomwe nakumbukila kuti zintu zimenezi
zinalembedwa ndi ie, ndimo kuti anatshita zintu zimenezi
kwa ie. Ndimo antu ambiri omwe anali nai' ntawi anaitana 17
Lazaro kwa mwanda, namukitsa kwa akufa, namariza.
Kwa tshifukwa tshimenetshi inso antu ambiri nang'ka 18
nakomana nai', tshifuka anamva kuti anatshita tshizindikilo
tshimene. Ndimo Afarisi nauzana, Muonetsa bwanje mupa- 19
mbana palibe kantu: ona, dziko linatsatana nai'.

Ndimo kunali Agrike mwa awa omwe anakwera ku pe- 20

21 mbedza pa kudia: ndimo amene nafika ku Filipu, emwe
anali wa Betsayida wa Galileya, namfunsa, kuti, Fumu,
22 tifuna ku ona Yesu. Filipu afika nauza Andreya: Andreya
23 adza, ndi Filipu, ndimo auza Yesu. Ndimo Yesu aiang'ka
awo, kuti, Ora lafika, monga kuti Mwana wa muntu akapa-
24 mbanitsidwa. Dinena ndi inu nditu, nditu, Kani mpetshe
ya dzintu igwa muntaka nifa, nikala yoka; koma ngati ifa,
25 ibala dzobala dzambiri. Iemwe akonda moyo watshi auta-
ia; ndimo iemwe akwia ndi moyo watshi m' dziko limene
26 adzausunga ku moyo wosamariza. Ngati muntu modzi
andiimirira, anditsate; ndimo kuti diri, pomwe woimirira
wanga adzali inso: ngati muntu modzi andiimirira, ie Atate
27 adzamlemekeza. Tsopano nzimu wanga untentemeredwa;
ndimo didzanena tshiani? Atate, pulumutsa ine kwa ora
limene. Koma kwa tshifukwa tshimene dinafika kwa ora
28 limene. Atate, pambanitsa dzina lako. Ndimo liu linadzera
kumwamba, *kuti*, Dalipambanitsa, ndimo didzalipambanitsa
29 anso. Ndimo antu ambiri, omwe naima pafupi, nalimva,
nati kuti linali bingu: ena nati, Njelo walankula nai'.
30 Yesu naiang'ka nati, Liu limene silinafika tshifuka kwa ine,
31 koma kwa inu. Tsopano kuli kuweruza kwa dziko limene:
32 tsopano woweruza wa dziko limene adzaturutsidwa. Ndimo
ine, ngati ditukulidwa kwa dziko, didzakoka antu onse kwa
33 ine ndeka. Koma tshimene nanena, kusonyeza ndi imfa
34 yanje akafa. Ndimo antu ambiri naiang'ka ie, Tamva kwa
mau kuti Kristu akala dzaka dzonse: ndimo unena bwanje,
Mwana wa muntu akanatukulidwa? Mwana wa muntu
35 amene ali ani? Ndimo Yesu nanena nao, Ntawi yeing'ono
kosuntira kuunika kuli mwa inu. Endaendani ntawi mupo-
tshera kuunika, kuti ndima usagwira inu: ndimo iemwe
36 aendaenda mudima wosadziwa pomwe ang'ka. Ntawi mu-
potshera kuunika, mvanani ndi kuunika, kuti mungokala
ana a kuunika.

Zintu zimenezi Yesu nalankula, namuka nabisala eka kwa
37 awo. Koma kuti anatshita zizindikilo zambiri patsogolo
38 pa awo, sanamvana ndi ie: monga kuti mau a Yesaya
mprofeti anangodzazidwa, omwe nanena,

Mwini, mbiri yatu wamvana ndani?
Ndimo kwa ani nkono wa Mwini wasonyezedwa?

39 Kwa tshifukwa tshimene sanadziwa ku mvana, tshifuka kuti
Yesaya nanena anso,

40 Watseketsa maso ao, nalimbikitsa mitima yao;

Kani akaona ndi maso ao, ndimo akadziwitsa ndi mitima yao,
Ndimo akatembenuka,
Ndimo dikatshiritsa awo.

Zintu zimenezi nazinena Yesaya, tshifuka naona kupambana 41
kwatshi; nalankula ndi ie. Koma inde mwa oweruza 42
ambiri anamvana ndi ie; koma tshifuka tsha Afarisi sana-
bvomera *ie*, kani akaturutsidwa mwa sinagoge: kuti na- 43
konda kupambana kwa antu kopambana kupambana kwa
Mulungu.

Ndimo Yesu napfula nati, Iemwe amvana ndi ine, wosa- 44
mvana ndi ine, koma ndi ie emwe ananditumiza. Ndimo 45
iemwe aona ine aona ie emwe ananditumiza. Dafika kuu- 46
nika m' dziko, kuti iemwe amvana ndi ine wosangokala
mudima. Ndimo ngati muntu modzi amva mau anga, 47
ndimo wosasunga, sindimweruza: kuti sindinafika ku weruza
dziko, koma ku pulumutsa dziko. Iemwe akana ine, ndimo 48
wosalandira mau anga, ali ndi modzi emwe amweruza: mau
omwe dinalankula, omwe adzamweruza m' dzua lomariza.
Kuti sindinalankula kwa ine ndeka; koma Atate emwe 49
ananditumiza, wandipatsa mau, omwe dikanena, ndi omwe
dikalankula. Ndimo didziwa kuti mau atshi ali moyo wosa- 50
mariza: ndimo zintu zomwe dilankula, inde modzimodzi
Atate wandiuza, tshointshi dilankula.

Ndimo patsogolo kudia kwa mpasika, Yesu kudziwa kuti 13
ora latshi linafika kuti akaturuka m' dziko limene kwa
Atate, anakonda atshi omwe anali m' dziko, nakonda awo
ku nsonga. Ndimo pa ngonero, diabolos kali anaika muti- 2
ma wa Yuda Sikariyoti, *mwana* wa Simon, kumzonda,
*Yesu*, kudziwa kuti Atate anapatsa zintu zonse m' manja 3
mwatshi, ndimo kuti nadzera kwa Mulungu, ndimo ang'ka
kwa Mulungu, auka kwa ngonero, ndimo aika miinjiro 4
yatshi; natenga nsaru yopukutira, nadzimangitsa. Ndimo 5
atsanula madzi m' mbale, naamba ku tsuka mapazi a akupu-
nzira, ndi ku pukuta awa ndi nsaru yopukutira yomwe
anamanga. Ndimo afika ku Simon Petros. Anena nai', 6
Mwini, kodi utsuka mapazi anga? Yesu naiang'ka nanena 7
nai', Tshomwe ditshita usadziwa tsopano; koma udzadziwitsa
pambuiu. Petros anena nai', Usatsuka mapazi anga palibe 8
ntawi. Yesu naiang'ka ie, Ngati sindikutsuka, usapotshera
kantu ndi ine. Simon Petros anena nai', Mwini, si mapazi 9
anga oka, koma anso manja anga ndi mutu wanga. Yesu 10

anena nai', Iemwe wasambitsidwa wosafuna koma ku tsuka
mapazi atshi, koma ali wotsuka iense: ndimo muli otsuka,
11 koma si onse. Kuti nadziwa iemwe akamzonda; ndimo
nanena, Musali otsuka onse.
12 Ndimo ntawi anatsuka mapazi ao, natenga miinjiro yatshi,
nakala pansi inso, nanena nao, Kodi mudziwa tshiani datshi-
13 ta ndi inu? Munditsha, Mpunzitsi, ndi, Mwini: ndimo
14 munena bwino; kuti ndiri. Ndimo ngati ine, Mwini ndi
Mpunzitsi, datsuka mapazi anu, inu unso mukanatsukana
15 mapazi anu. Kuti dapatsa inu sonyezo, kuti inu unso
16 mukatshita monga datshita ndi inu. Dinena ndi inu nditu,
nditu, Kapolo wosali wang'kuru ndi mwini watshi; kapena
17 wotumidwa wang'kuru ndi iemwe anamtumiza. Ngati mu-
dziwa zintu zimenezi, odala muli inu ngati muzitshita.
18 Sindinena ndi inu nonse: didziwa omwe dasang'ka: koma
monga kuti lemba lingodzazidwa, Iemwe adia nkate wanga
19 anatukula tshitende tshatshi pa ine. Kwa tsopano diuza
inu patsogolo tshidzakala, kuti, ntawi tshikala, mungomvana
20 kuti diri *ie*. Dinena ndi inu nditu, nditu, Iemwe alandira
iemwe dituma alandira ine; ndimo iemwe alandira ine
alandira iemwe ananndituma.
21 Ntawi Yesu ananena tshointshi, nantentemeretsedwa
mutima, namariza, nati, Dinena ndi inu nditu, nditu, kuti
22 modzi wa inu adzandizonda. Akupunzira anayang'ana
23 modzi pa wina, kuganizaganiza ndi ani nanena. Anali pa
gome kutsamira pa tshifua tsha Yesu modzi wa akupunzira
24 atshi, emwe Yesu nakonda. Ndimo Simon Petros akodola
kwa ie, ndimo anena nai', *Ti*uze ndani ali ndi emwe anena.
25 Ndimo ie alikutsamira, monga anali, pa tshifua tsha Yesu
26 anena nai', Mwini, ali ani? Ndimo Yesu aiang'ka, Ali ie,
kwa emwe didzasunsira kang'ono, ndimo didzakapatsa ie.
Ndimo ntawi anasunsa kang'ono, akatenga, nakapatsa kwa
27 Yuda, *mwana* wa Simon Sikariyoti. Ndimo pambuiu
kang'ono, pomwe Satana anamloa. Ndimo Yesu anena nai',
28 Tshomwe utshita, tshita nsanga. Ndimo kulibe muntu pa
gome nadziwa kwa tshifukwa tshiani nanena amene ndi ie.
29 Kuti ena naganiza, tshifuka Yuda anali ndi tumba, kuti
Yesu ananena nai', Gulitsa zintu zomwe tiri ndi kufunidwa
ndi kwa kudia; kapena, kuti akapatsa kantu kwa osauka.
30 Ndimo analandira kang'ono naturuka tsopano lino: ndimo
unali usiku.
31 Ndimo ntawi anaturuka, Yesu ati, Tsopano Mwana wa

muntu apambanitsidwa, ndimo Mulungu apambanitsidwa
mwa ie; ndimo Mulungu adzampambanitsa mwa ie eka, 32
ndimo tsopano lino adzapambanitsa ie. Tiana, iripo ntawi 33
yeing'ono dikala ndi inu. Mudzandifuna: ndimo monga
dinanena ndi Ayuda, Kuti ding'ka, musadziwa ku fika; tshoi-
ntshi tsopano dinena ndi inu. Mau atsopano dipatsa inu, 34
kuti mukondana; inde monga dakonda inu, kuti inu unso
mukondana. Ndi tshimene antu onse adzadziwa kuti muli 35
akupunzira anga, ngati mupotshera kukondana.
Simon Petros anena nai', Mwini, ung'ka kuti? Yesu naia- 36
ng'ka, Komwe ding'ka, usadziwa kunditsata tsopano; koma
udzatsata pambuiu. Petros anena nai', Mwini, sindidziwa 37
ku tsata iwe inde tsopano bwanje? Kwa iwe didzaika pansi
moyo wanga. Yesu aiang'ka, Kodi udzaika moyo wako kwa 38
ine? Dikuuza nditu, nditu, Tambala sadzalira, kwa ntawi
udzandikana katatu.
Musantuntumira ntima yanu: mumvana ndi Mulungu, 14
mvanani inso ndi ine. M' nyumba ya Atatu anga alipo 2
malo okala ambiri; ngati si tshointsho, dikanakuuzani;
kuti ding'ka ku konzetsa malo kwa inu. Ndimo ngati 3
ding'ka ndikonzetsa malo kwa inu, dibwera, ndidzalandira inu
kwa ine ndeka; kuti, pomwe diri, *apo* mungokala anso. Ndimo 4
kuti ding'ka, mudziwa njira. Tomas anena nai', Mwini, 5
sitidziwa kuti umuka; tidziwa njira bwanje? Yesu anena 6
nai', Diri njira, ndi nteradi, ndi moyo: palibe modzi adza
kwa Atate, koma ndi ine. Ngati munandidziwa, mukana- 7
dziwa Atatu anga anso: kwa ntawi yatsopano mumdziwa,
ndi munamona. Filipu anena nai', Mwini, utisonyeza Atate, 8
ndimo atidzaza. Yesu anena nai', Kodi dakala ntawi 9
yambiri ndi iwe, ndimo usandidziwa, Filipu? iemwe
wandiona waona Atate; unena bwanje, Utisonyeza Atate?
Kodi sumvana kuti diri mwa Atate, ndi Atate mwa ine? 10
mau omwe dinena ndi inu dilankula si kwa ine ndeka:
koma Atate kukala mwa ine atshita ntshito zatshi. Mvanani 11
ine kuti diri mwa Atate, ndi Atate mwa ine: kapena
mvanani ine tshifuka tsha ntshito zoka. Dinena ndi inu, 12
nditu, nditu, Iemwe amvana ndi ine, ntshito zomwe ditshita
adzatshita anso; ndimo *ntshito* zopambana izo adzatshita;
tshifuka ding'ka kwa Atate. Ndimo tshomwe mudzafunsa 13
m' dzina langa, tshomwe didzatshita, monga kuti Atate
angopambanitsidwa mwa Mwana. Ngati udzafunsa ine 14
kantu m' dzina langa, didzatshitshita. Ngati mukonda 15

16 ine, mudzasunga mau anga. Ndimo didzapempera Atate,
ndimo adzapatsa inu Wosangalatsa wina, kuti angokala
17 ndi inu dzaka dzosamariza, *inde* Nzimu wa nteradi: womwe
dziko losadziwa ku landira; tshifuka kuti losauona, kapena
losaudziwa: muudziwa iwo; kuti ukala ndi inu, ndimo
18 udzali mwa inu. Sindidzasia inu ampawi: didza kwa inu.
19 Iripo ntawi yeing'ono, ndimo dziko losandiona palibe ntawi
ina; koma mundiona: tshifuka dikala ndi moyo, mudzakala
20 ndi moyo onso. Mwa siku ilo mudzadziwa kuti diri mwa
21 Atatu anga, ndi inu mwa ine, ndi ine mwa inu. Iemwe
apotshera mau anga, nasunga awa, ie ali emwe akonda ine:
ndimo iemwe andikonda adzakondedwa ndi Atatu anga,
ndimo didzakonda ie, ndimo didzasonyeza ine ndeka kwa ie.
22 Yuda (si Sikariyoti) anena nai', Mwini, tshakala tshiani kuti
23 udzasonyeza iwe eka kwa ife, ndimo si kwa dziko? Yesu
naiang'ka nanena nai', Ngati muntu andikonda, adzasunga
mau anga: ndimo Atatu anga adzamkonda, ndimo tidzafika
24 kwa ie, ndimo tidzakala nai'. Iemwe wosandikonda wosasu-
nga mau anga: ndimo mau omwe mumva osali anga, koma
a Atate emwe ananditumiza.

25 Zintu zimenezi dalankula ndi inu, ntawi dirikukala ndi
26 inu. Koma Wosangalatsa, *inde* Nzimu Woyera, womwe
Atate adzatumiza m' dzina langa, iwo udzapunzitsa inu
zintu zonse, nudzakumbukilitsa inu zonse zomwe dinanena
27 ndi inu. Ntendere disiira inu; ntendere wanga dipatsa ku inu:
si monga dziko lipatsa, dipatsa kwa inu. Musantuntumira
28 ntima wanu, kapena musatshita manta. Munamva bwanje
danena ndi inu, Dimuka, ndimo didza kwa inu. Ngati muli-
kukonda ine, mukanasekera, tshifuka ding'ka kwa Atate:
29 kuti Atate ali wang'kuru ndi ine. Ndimo tsopano dauza
inu patsogolo kudzali, kuti, ntawi kunali, mungomvana.
30 Pambuiu sindilankula kwambiri ndi inu, kuti woweruza wa
dziko adza: ndimo apotshera tshabe mwa ine; koma kuti
dziko lingodziwa kuti dikonda Atate, ndimo monga Atate
anandipatsa mau, inde tshimwetshi ditshita. Ukani, tidzi-
ng'ka uko.

15 Diri mvina woona, ndi Atatu anga ali wotshita munda.
2 Mitawi yonse mwa ine yomwe yosabala dzobala, aitshotsa:
ndi yonse yomwe ibala dzobala, aifotokoza, monga kuti
3 ingobala dzobala dzopambana. Tsopano mufotokozedwa
4 tshifuka tsha mau omwe dalankula ndi inu. Kalani mwa
ine, ndi ine mwa inu. Monga ntawi wosadziwa woka ku

bala dzobala, kani ukala mwa mvina; monga kapena si inu,
kani mukala mwa ine. Diri mvina, muli mitawi: Iemwe 5
akala mwa ine, ndi ine mwa ie, emwe abala dzobala dza-
mbiri; kuti obaluka ine musadziwa ku tshita kantu. Ngati 6
muntu wosakala mwa ine, aturutsidwa modzimodzi ndi
ntawi, ndimo aumidwa; ndimo aunjika iyo, ndimo aponya
iyo pa moto, ndimo iotshedwa. Ngati mukala mwa ine, ndi 7
mau anga akala mwa inu, funsani tshomwe mufuna, ndimo
adzatshitshitidwa kwa inu. M' tshimene Atatu anga apamba- 8
nitsidwa, kuti mubala dzobala dzambiri; ndimo *tshointshi*
mudzali akupunzira anga. Inde monga Atate wandikonda, 9
ine enso dakonda inu: kalani m' kukonda kwanga. Ngati 10
musunga mau anga, mudzakala m' kukonda kwanga; inde
monga dasunga mau a Atatu anga, ndimo dikala m' kuko-
nda kwatshi. Zintu zimenezi dalankula ndi inu, kuti 11
tshimwemwe tshanga tshingokala mwa inu, ndimo *kuti*
tshimwemwe tshanu tshingodzazidwa. Amene ali mau anga, 12
kuti mukondane, inde monga dakonda inu. Palibe muntu 13
ali ndi kukonda kopambana kumene, kuti muntu adzafera
kwa abali atshi. Muli abali anga, ngati mutshita zintu 14
zomwe diuza inu. Ntawi ina sinditsha inu akapolo; tshi- 15
fuka kapolo wosadziwa tshomwe mwini watshi atshita: koma
datsha inu abali; kuti zintu zonse zomwe dinamva kwa
Atatu anga dinauza inu. Usasang'ka ine, koma dinasang'ka 16
inu, ndimo dinaika inu, kuti mukaenda ndimo mukabala
dzobala, ndimo *kuti* dzobala dzanu dzikakala: kuti kantu
komwe mudzafunsa kwa Atate m' dzina langa, ango- 17
patsa inu. Zintu zimenezi dikuuzani, kuti mukondane.
Ngati dziko likwiira inu, mudziwa kuti lakwiira ine patso- 18
golo *linakwiira* inu. Ngati munali a dziko, dziko likakonda 19
latshi: koma tshifuka simuli a dziko, koma dinasang'ka inu
kwa dziko, tshointsho dziko likwiira inu. Kumbukilani 20
mau omwe dinanena ndi inu, Kapolo wosali wopambana
mwini watshi. Ngati anazunza ine, adzazunza inu unso;
ngati anasunga mau anga, adzasunga anu unso. Koma 21
zintu zonse zimene adzatshita kwa inu kwa dzina langa, tshi-
fuka osadziwa emwe ananditumiza. Ngati sindinadza ndimo 22
sindinalankula nao, sakanapotshera mpulupulu: koma tsopano
ali ndi palibe kubvumbuka kwa mpulupulu zao. Iemwe 23
akwiira ine akwiira Atatu anga anso. Ngati sindina- 24
tshita mwa awa ntshito zomwe kulibe muntu wina ana-
tshita, sakanapotshera mpulupulu: koma tsopano anaona

25 anakwira ine ndi Atatu anga. Koma *tshimene tshiri*, kuti
mau angodzazidwa omwe alembedwa m' mau ao, Anakwiira
26 ine kopanda tshifukwa. Koma ntawi Wosangalatsa adzadza,
emwe didzatumiza kwa inu kwa Atate, *inde* Nzimu wa nte-
radi, womwe uturuka kwa Atate, udzamariza ndi ine:
27 ndimo inu unso mumariza, tshifuka munali ndi ine kwa
kuamba.

16 Zintu zimenezi dalankula ndi inu, kuti simunganakwii-
2 tsidwa. Adzaturutsa inu mwa masinagoge: inde ora lifika,
kuti iemwe apa inu adzaganiza kuti agwira ntshito ya
3 Mulungu. Ndimo zintu zimenezi adzatshita, tshifuka kuti
4 sanadziwa Atate, kapena ine. Koma zintu zimenezi daku-
lankulani, monga kuti ntawi ora lao linafika, mungokumbu-
kila izo, bwanje kuti dakuuzani. Ndi zintu zimenezi
sindinanena ndi inu kwa kuamba, tshifuka dinali ndi inu.
5 Koma tsopano ding'ka kwa iemwe ananditumiza; ndi palibe
6 modzi wa inu andifunsa, Ung'ka kuti? Koma tshifuka
dalankula zintu zimenezi kwa inu, tshisoni tshadzaza
7 ntima wanu. Koma dinena ndi inu nteradi; Tshiri
tshabwino kwa inu kuti dimuka: kuti ngati sindi-
muka, Wosangalatsa sadzafika kwa inu; koma ngati dimuka,
8 didzamtumiza kwa inu. Ndimo ie, ntawi nafika, adzasutsa
9 dziko ndi mpulupulu, ndi kudeka, ndi kuweruza: ndi
10 mpulupulu, tshifuka osamvana ndi ine; ndi kudeka,
tshifuka ding'ka ku Atate, ndimo musaona ine enso;
11 ndi kuweruza, tshifuka woweruza wa dziko limene
12 anaweruzidwa. Dipotshera kosuntira zintu zambiri ku
13 nena ndi inu, koma musadziwa kuzimva tsopano. Koma
ntawi iwo, Nzimu wa nteradi, unadza, udzatsogolera inu ku
nteradi wonse: kuti sudzalankula ndi iwo oka; koma
zintu zomwe udzamva, udzalankula: ndimo udzauza inu
14 zintu zomwe zidzadza. Udzapambanitsa ine: kuti udzatenga
15 ndi zanga, ndimo udzauza inu. Zintu zonse zomwe Atate
apotshera ziri zanga: ndimo dinanena, kuti utenga ndi
16 zanga nudzauza inu. Ntawi yeing'ono, ndimo simundiona
anso; ndimo onso ntawi yeing'ono, ndimo mudzandiona.
17 Ndimo *ena* a akupunzira atshi nauzana, Tshimene tshiri
tshiani tshomwe anena ndi ife, Ntawi yeing'ono, ndimo
simundiona; ndimo onso ntawi yeing'ono, ndimo
mudzandiona: ndi, Tshifuka kuti ding'ka kwa Atate?
18 Ndimo nanena, Tshimene tshiri tshiani tshomwe anena,
19 Ntawi yeing'ono? Sitidziwa tshomwe alankula. Yesu

nadziwitsa kuti anafuna kumfunsa, ndimo nanena nao,
Kodi mufunsana ndi tshimene, tshomwe dinanena, Ntawi
yeing'ono, ndimo simundiona, ndimo onso ntawi yeing'ono,
ndimo mudzandiona? Dinena ndi inu, nditu, nditu, kuti 20
mudzalira misozi ndi mudzapfula, koma dziko lidzasekera:
mudzakala ndi tshisoni, koma tshisoni tshanu tshidzatembe-
nuzidwa kwa tshimwemwe. Nkazi ntawi alikubala akala 21
ndi tshisoni, tshifuka kuti ora latshi linafika: koma ntawi
anabala kamwana, sanakumbukila anso tshisoni, kuti
tshimwemwe kuti mamuna anabadwa m' dziko. Ndimo 22
tsopano muli ndi tshisoni: koma didzakuonani inso, ndimo
ntima wanu udzasekera, ndi tshimwemwe tshanu palibe
modzi atshotsa kwa inu. Ndimo mwa dzua limenelo simu- 23
dzandifunsa kantu. Dinena ndi inu, nditu, nditu, Ngati
mudzafunsa kantu kwa Atate, adzakupatsani m' dzina langa.
Ntawi inapita simunafunsa kantu m' dzina langa: funsani, 24
ndimo mudzalandira, kuti tshimwemwe tshanu tshingo-
dzazidwa.

Zintu zimenezi dalankula ndi inu m' mafanizo: ora lidza, 25
ntawi sindidzalankula anso kwa inu m' mafanizo, koma
didzauza inu poyera ndi Atate. M' dzua limene mudzafunsa 26
m' dzina langa: ndimo sindinena ndi inu, kuti didzapempa
Atate kwa inu; kuti Atate oka akonda inu, tshifuka kuti 27
munandikonda, ndi munamvana kuti dinaturuka kwa Atate.
Dinaturuka kwa Atate, ndaloa m' dziko: onso, dileka dziko, 28
nding'ka ku Atate. Akupunzira atshi ati, Ona, tsopano 29
ulankula koona, ndimo usanena fanizo. Tsopano tidziwa 30
kuti udziwa zintu zonse, ndimo usafuna kuti muntu modzi
akafunsa iwe: ndi tshimene timvana kuti unaturuka kwa
Mulungu. Yesu naiang'ka awo, Kodi mumvana tsopano? 31
Ona, ora lidza, inde, lafika, lomwe mudzabalalitsidwa, antu 32
onse kwao, nadzasia ine ndeka: koma sindiri ndeka,
tshifuka kuti Atate ali ndi ine. Zintu zimenezi dalankula 33
ndi inu, kuti mwa ine mungopotshera ntendere. M' dziko
mudzapotshera sautso: koma kalani osekera; dapambana
dziko.

17
Zintu zimene Yesu nalankula; ndimo kutukula maso
atshi ku mwamba, nati, Atate, ora linadza; pambanitsa
Mwana wako, kuti Mwana angopambanitsa iwe: inde monga 2
unampatsa mpamvu pa nyama zonse, kuti tshomwe wampa-
tsa, ku awo akapatsa moyo wosamariza. Ndimo tshimene 3
tshiri moyo wosamariza, kuti akadziwa iwe Mulungu woona

4 eka, ndi iemwe unatumiza, *inde* Yesu Kristu. Dinapamba-
nitsa iwe pa dziko, kunata ntshito yomwe unandipatsa
5 ku tshita. Ndimo tsopano, Atate, pambanitsa ine ndi iwe
eka ndi kupambana komwe dinapotshera ndi iwe patsogolo
6 pa dziko linali. Dinasonyeza dzina lako kwa antu omwe
unandipatsa kwa dziko: ako anali, ndimo unandipatsa awo;
7 ndimo anasungira mau ako. Tsopano adziwa kuti zintu
8 zonse zomwe wandipatsa ziri kwa iwe: kuti mau omwe
unandipatsa dapatsa ku awa; ndimo analandira, nadziwa
ndi nteradi kuti dinaturuka kwa iwe, namvana kuti
9 unatumiza ine. Dipempera awo: sindipempera dziko,
10 koma kwa omwe wandipatsa; kuti ali ako: ndi zintu zonse
zomwe ziri zanga ziri zako, ndi zako ziri zanga: ndimo
11 dipambanitsidwa mwa awo. Ndimo sindiri ntawi ina m'
dziko, ndimo amene ali m' dziko, ndimo didza kwa iwe. Atate
Woyera, sunga awo m' dzina lako omwe wandipatsa, kuti
12 angokala modzi, inde monga ti*ri*. Ntawi dinali nao,
dinasunga awo m' dzina lako omwe wandipatsa: ndinasungira
awo, ndimo kulibe modzi wa awo namwazika, koma mwana
13 wa kumwazika; kuti lemba linangodzazidwa. Koma
tsopano difika kwa iwe; ndi zintu zimenezi dilankula m'
dziko, kuti angopotshera tshimwemwe tshanga tshadzazidwa
14 mwa awo oka. Dapatsa awo mau ako; ndimo dziko
linakwiira awo, tshifuka osali a dziko, inde monga sindiri
15 wa dziko. Sindipempa kuti ukatshotsa awo kwa dziko,
16 koma kuti ukasungira awo kwa *wa*mpulupulu. Osali a dziko,
17 inde monga sindiri wa dziko. Yeretsa awo mwa nteradi:
18 mau ako ali nteradi. Monga unanditumiza m' dziko, inde
19 tshointshi dinatumiza awo m' dziko. Ndimo kwa awo diye-
retsa ine ndeka, kuti awo oka anso angoyeretsedwa ndi
20 nteradi. Sindipempera awo oka, koma kwa awo onso omwe
21 amvana ndi ine mwa mau ao; kuti onsewo angokala modzi;
inde monga iwe, Atate, *uli* mwa ine, ndi ine mwa iwe, kuti
awo onso angokala mwa ife: kuti dziko lingomvana kuti
22 unanditumiza. Ndi kupambana komwe wandipatsa dapatsa
23 kwa awo; kuti angokala modzi, inde monga ti*ri* modzi; ine
mwa awo, ndi iwe mwa ine, kuti angopangidwa akuta mwa
modzi; kuti dziko lingodziwa kuti unanditumiza, ndimo
24 unakonda awo, inde monga unakonda ine. Atate, omwe
wandipatsa, difuna kuti, pomwe diri, awo onso angokala ndi
ine; kuti angoona kupambana kwanga, komwe wandipatsa:
25 kuti unandikonda patsogolo pa kuzika kwa dziko. O Atate,

wodeka, dziko silinadziwa iwe, koma dinadziwa iwe; ndi
amenewa nadziwa kuti unanditumiza; ndimo dinauza awo 26
dzina lako, ndimo didzauza; kuti kukonda ndi komwe una-
ndikonda kungokala mwa awo, ndi ine mwa awo.

Ntawi Yesu ananena mau amene, naturuka ndi akupu- 18
nzira atshi patsidia lina la kantsinje Kidron, pomwe panali
munda, momwe naloa, ie eka ndi akupunzira atshi. Ndimo 2
Yuda anso, iemwe nazonda ie, nadziwa malo: kuti Yesu
kawiri kawiri nang'ka uko ndi akupunzira atshi. Ndimo 3
Yuda, analandira gulu *la ankhondo*, ndi akazembe kwa
adzukuru akuru ndi Afarisi, adza apo ndi nyali ndi miuni
ndi mauta. Ndimo Yesu, kudziwa zintu zonse zomwe 4
zirinkudza pa ie, naturuka, ndimo anena nao, Mufuna ani?
Naiang'ka ie, Yesu wa Nazarete. Yesu anena nao, Diri. 5
Ndi Yuda anso, emwe nazonda ie, analikuima nao. Ndimo 6
ntawi nanena nao, Diri, nabwerera, nagwa pansi. Ndimo 7
nafunsa awo onso, Mufuna ani? Nati, Yesu wa Nazarete.
Yesu naiang'ka, Dinakuuzani kuti ndiri: ndimo ngati mu- 8
ndifuna, lekani amenewa ku muka: kuti mau anangodzazi- 9
dwa omwe nanena, Wa omwe wandipatsa dinataia palibe
modzi. Ndimo Simon Petros anali ndi mpeni wa nkondo 10
nauturutsa, nakoma kapolo wa ndzukuru wang'kuru, nadula
kutu latshi lamanja. Ndimo dzina la kapolo linali Malko.
Ndimo Yesu nanena ndi Petros, Loetsa mpeni wa nkondo m' 11
banzi latshi: tshiko tshomwe Atate wandipatsa, kodi sindi-
mwera itsho?

Ndimo gulu ndi kazembe wang'kuru, ndi akazembe a 12
Ayuda, nagwira Yesu nammanga, namtsogoza ku Hana 13
pakuamba; kuti anali pongozi wa Kayafa, emwe anali ndzu-
kuru wang'kuru tshaka tshimene. Ndimo Kayafa anali 14
iemwe naweruza Ayuda, kuti kunali kwabwino kuti muntu
modzi akafera antu.

Ndimo Simon Petros natsata Yesu, ndi wopunzira wina. 15
Ndimo wopunzira amene anadziwidwa ndi ndzukuru wang'-
kuru, naloa ndi Yesu m' bwalo la ndzukuru wang'kuru;
koma Petros analikuima pa komo kunja. Ndimo wopunzira 16
wina, emwe anadziwidwa ndi ndzukuru wang'kuru, naturuka
nanena ndi iemwe anayang'anira komo, naloetsa Petros.
Ndimo butu lomwe linayang'anira komo linena ndi Petros, 17
Kodi suli inso *modzi* wa akupunzira a muntu amene?
Anena, Sindiri. Ndimo akapolo ndi akazembe analikuima 18
*apo*, anapanga moto wa makala; kuti kunali kuzizira;

ndimo analikuota awa oka: ndimo Petros anso anali nao,
kuima kuota ie eka.
19 Ndimo ndzukuru wang'kuru nafunsa Yesu ndi akupunzira
20 atshi, ndi kwa kupunzitsa kwatshi. Yesu naiang'ka ie,
Dalankula poyera ku dziko; ntawi yonse dinapunzitsa m'
masinagoge, ndi m' tempile, komwe Ayuda onse asong'kana;
21 ndi m' tseri sindinalankula kantu. Undifunsa bwanje?
funsa awo omwe ana*ndi*mva, tshomwe dinalankula nao:
22 ona, amene adziwa zintu zomwe dinanena. Ndimo ntawi
ananena zimenezi, modzi wa akazembe kuima pafupi na-
menya Yesu ndi tshikatu tshatshi, kuti, Suiang'ka ndzukuru
23 wang'kuru tshointshi? Yesu naiang'ka ie, Ngati dalankula
tshoipa, mariza ndi tshoipa: koma ngati tshabwino, undi-
24 menya bwanje? Ndimo Hana anamtumiza womangidwa
ku Kayafa ndzukuru wang'kuru.
25 Ndimo Simon Petros analikuima kuota ie eka. Ndimo
nanena nai', Suli inso *modzi* wa akupunzira atshi? Nakana,
26 nati, Sindiri. Modzi wa akapolo a ndzukuru wang'kuru,
ali mbali wa ie emwe Petros nadula kutu latshi, ati, Kodi
27 sindinakuona m' munda nai'? Ndimo Petros nakana anso:
ndimo tsopano lino tambala nalira.
28 Ndimo atsogoza Yesu kwa Kayafa ku Pretorium: ndimo
kunali mamawa; ndi awa oka sanaloa m' Pretorium, kuti
29 siangoipitsidwa, koma anangodia mpasika. Ndimo Pilato
naturuka ku awo, ndimo ati, Tshulo lanje mutenga pa
30 muntu amene? Naiang'ka nanena nai', Ngati muntu amene
31 sanali wotshita zoipa, sitikanapereka ie kwa iwe. Ndimo
Pilato nanena nao, Tengani ie, ndi weruzani ie kofana ndi
mau anu. Ndimo Ayuda nanena nai', Sitshiri tshamau kwa
32 ife ku pa muntu modzi: kuti mau a Yesu anangodzazidwa,
omwe nanena, kusonya ndi imfa yanje akafa.
33 Ndimo Pilato naloa anso m' Pretorium, naitana Yesu,
34 nanena nai', Kodi uli Fumu Yotshuka ya Ayuda? Yesu
naiang'ka, Kodi unena tshimene ndi iwe eka, kapena ena
35 anakuuza tshimene ndi ine? Pilato naiang'ka, Diri Myuda
kodi? Mtundu wako ndi adzukuru akuru anakupereka
36 kwa ine: watshita tshiani? Yesu naiang'ka, Dziko langa
siliri la dziko lino: ngati dziko langa linali la dziko lino,
akapolo anga akapanga nkondo, kuti sindikaperekedwa kwa
37 Ayuda: koma tsopano dziko langa siliri la kuno. Ndimo
Pilato nanena nai', Kodi uli pomwe fumu yotshuka? Yesu
naiang'ka, Unena kuti diri fumu yotshuka. Kwa nsonga

imene dabadwa, ndi kwa nsonga imene dafika m' dziko,
kuti dikamariza ndi nteradi. Omwe ali a nteradi amva liu
langa. Pilato anena nai', Nteradi uli tshiani? 38
Ndimo ntawi ananena tshimene, naturuka anso kwa Ayuda,
ndimo anena nao, Dipeza kulibe tshimo mwa ie. Koma 39
muli ndi ntengo, kuti dikamasula modzi kwa inu pa
mpasika: kodi mufuna kuti didzamasula kwa inu Fumu
Yotshuka ya Ayuda? Ndimo napfula anso, kuti, Si muntu 40
amene, koma Baraba. Ndimo Baraba anali wolanda.
Ndimo pomwe Pilato natenga Yesu, nakwapula ie. 19
Ndimo ankhondo naluka tshisoti tshotshuka tsha minga, 2
natshiika pa mutu patshi, nabveka ie ndi mwinjiro wakuda;
ndimo nadza kwa ie, nati, A, Fumu Yotshuka ya Ayuda! 3
nammenya ndi manja ao. Ndimo Pilato naturuka anso, 4
ndimo anena nao, Onani, diturutsa ie kwa inu, monga kuti
mudziwe kuti dipeza mwa ie mulibe tshimo. Ndimo Yesu 5
naturuka, kubvala tshisoti tshotshuka tsha minga ndi mwi-
njiro wakuda. Ndimo *Pilato* anena nao, Onani, muntu!
Ndimo ntawi adzukuru akuru ndi akazembe anamona, 6
napfula, kuti, Patshika *ie*, patshika *ie*. Pilato anena nao,
Tengani ie, ndimo patshikani ie: kuti dipeza mwa ie mulibe
tshimo. Ayuda anaiang'ka ie, Tiri ndi mau, ndimo ndi 7
mau amene akanafa, tshifuka napanga ie eka Mwana wa
Mulungu. Ndimo ntawi Pilato anamva mau amene, ana- 8
opsedwa kopambana; naloa anso m' Pretorium, ndimo anena 9
ndi Yesu, Udzera kuti? Koma Yesu sanaiang'ka ie.
Ndimo Pilato anena nai', Sulankula ndi ine? sudziwa kuti 10
diri ndi mpamvu ku masula iwe, ndimo diri ndi mpamvu
ku patshika iwe? Yesu naiang'ka ie, Usadziwa ku potshera 11
mpamvu pa ine, kani kunapatsidwa kwa iwe kwa kumwa-
mba: ndimo iemwe anapereka ine kwa iwe anali ndi mpulu-
pulu yopambana. Pa tshimene Pilato nafuna ku masula ie: 12
koma Ayuda anapfula, kuti, Ngati umasula muntu amene,
usakala mbali wa Kesare: iemwe apanga ie eka fumu
yotshuka alankula pa Kesare. Ndimo ntawi Pilato anamva 13
mau amene, naturutsa Yesu, nakala pa mpando wa kuweruza
pa malo atshedwa Njira ya miala, koma m' Tshihebere,
Gabata. Ndimo kunali Kukonzetsa kwa mpasika: panali 14
pa ora latshisanu ndi tshimodzi. Ndimo anena ndi Ayuda,
Onani, Fumu Yotshuka yanu! Ndimo anapfula, Tshotsa *ie*, 15
tshotsa *ie*, patshika ie. Pilato anena nao, Kodi didzapatshika
Fumu Yotshuka yanu? Adzukuru akuru naiang'ka, Tiribe

16 fumu yotshuka koma Kesare. Ndimo pomwe nampereka
ku awo ku patshikidwa.
17 Ndimo natenga Yesu: ndimo naturuka, kunyamula
nkhwitshi kwa ie eka, kwa malo atshedwa Malo a pala,
18 omwe atshedwa m' Tshihebere Gologota: pomwe anapatshika
ie, ndimo ndi ie awiri ena, pa kundu lina modzi, pa kundu
19 lina wina, ndi Yesu pakati. Ndimo Pilato nalemba lemba
anso, naliika pa nkhwitshi. Ndimo kunalembedwa, YESU
20 WA NAZARETE, FUMU YOTSHUKA YA AYUDA. Ndimo lemba
limene ambiri a Ayuda anawerenga: tshifuka kuti malo
pomwe Yesu anapatshikidwa anali pafupi ku mzinda: ndimo
analembedwa ndi Tshihebere, *ndi* Tshiroma, *ndi* Tshigrike.
21 Ndimo adzukuru akuru a Ayuda nanena ndi Pilato,
Usalemba, Fumu Yotshuka ya Ayuda; koma, kuti anati,
22 Diri Fumu Yotshuka ya Ayuda. Pilato naiang'ka, Tshomwe
dalemba dalemba.
23 Ndimo ankhondo, ntawi anapatshika Yesu, natenga
miinjiro yatshi, napanga zidukwa zinai, ku wankhondo
modzi tshidukwa tshimodzi; ndi inso maraia: koma maraia
24 anali opanda nsono, oluka kumwamba pa onse. Ndimo
anauzana, Siting'ambe amene, koma tiyese kwa amene, wa
ani adzakala: kuti lemba linangodzazidwa, lomwe linena,

Nagawana miinjiro yanga,
Ndi kwa maraia anga anayesa.

25 Ndimo ankhondo anatshita zintu zimenezi. Koma mbali
wa nkhwitshi ya Yesu analikuima amai atshi, ndi mpwatshi
wa amai atshi, Mariya *nkazi* wa Kleyopa, ndi Mariya wa
26 Magadala. Ndimo ntawi Yesu naona amai atshi, ndi
wakupunzira kuima pafupi, emwe nakonda, anena ndi amai
27 atshi, Nkazi, ona, mwana wako! Ndimo anena ndi wa-
kupunzira, Ona, amai ako! Ndimo kwa ora limeneli
wakupunzira namtenga kwatshi.
28 Pambuiu tshimenetshi Yesu, kudziwa kuti zintu zonse
tsopano zata, kuti lemba linangodzazidwa, ati, Dimva ludzu.
29 Kunaikidwa apo tshiwira tshodzaza ndi vinegre: ndimo
naika sponje lodzaza ndi vinegre pa hisope, naika pa
30 nkamwa patshi. Ndimo ntawi Yesu analandira vinegre,
nati, Kwata: ndimo nawerama mutu watshi, nabweza nzimu
watshi.
31 Ndimo Ayuda, tshifuka kuti kunali Kukonzetsa, kuti
mitembo sikakala pa zinkhwitshi pa sabata (kuti dzua la
sabata limeneli linali *dzua* lalikuru), napempa Pilato kuti

miendo yao inangotsholedwa, ndimo kuti anangotshotsedwa.
Ndimo nadza ankhondo, natshola miendo ya tshimodzi, ndi 32
ya wina emwe anapatshikidwa nai': koma ntawi anadza 33
kwa Yesu, naona kuti wafa kali, sanatshola miendo yatshi:
koma modzi wa ankhondo ndi ntungu nalasa kundu latshi, 34
ndimo tsopano lino zinaturuka mwazi ndi madzi. Ndimo 35
iemwe waona, wamariza, ndi kumariza kwatshi kunali
koona: ndimo adziwa kuti anena kwanteradi, kuti inu unso
mungomvana. Kuti zintu zimenezi zinatshitidwa, kuti 36
lemba linangodzazidwa, Fupa la ie lisadzatsholedwa. Ndimo 37
onso lemba lina liti, Adzayang'ana ndi iemwe anambola.

Ndimo pambuiu zintu zimenezi Yosefe kwa Arimateya, 38
ali wopunzira wa Yesu, koma kutseri tshifuka tsha kuopa
kwa Ayuda, napempa Pilato kuti anangotshotsa ntembo wa
Yesu: ndimo Pilato nabvomera. Ndimo nadza, natshotsa
ntembo watshi. Nadza anso Nikodemo, iemwe patsogolo 39
nadza kwa ie usiku, kutenga zosang'kaniza za more ndi
akuzi, pa mapoundi makumi okaoka kumi *m' kulemera kwa-
tshi.* Ndimo natenga ntembo wa Yesu, naumanga ndi 40
nsaru za lini ndi zonung'kira, monga ntengo wa Ayuda uli
kuika m' mwanda. Ndimo pa malo pomwe anapatshi- 41
kidwa kunali munda; ndimo m' munda mwanda watsopano
momwe palibe muntu waikidwa ntawi yapita. Ndimo umo 42
tshifuka tsha Kukonzetsa kwa Ayuda (kuti mwanda unali
pafupi) anaika Yesu.

Ndimo pa *dzua* loamba la wiki adza Mariya kwa Maga- 20
dala m' mamawa, ntawi kosuntira kunali kuda, ku mwanda,
ndimo aona mwala watshotsedwa kwa mwanda. Ndimo 2
atamanga, nafika ku Simon Petros, ndi ku wopunzira wina,
emwe Yesu nakonda, ndimo anena nao, Anatshotsa Mwini
kwa mwanda, ndimo sitidziwa komwe anaika ie. Ndimo 3
Petros naturuka, ndi wopunzira wina, nang'ka ku mwanda.
Ndimo natamanga awiri: ndi wopunzira wina natamanga pa- 4
tsogolo Petros, nafika patsogolo ku mwanda; ndimo kusu- 5
zumira, aona nsaru za lini kukala; koma sanaloa. Ndimo 6
Simon Petros anso adza, kutsata ie, naloa m' mwanda; ndimo
aona nsaru za lini kukala, ndi mrenzo, womwe unali pa 7
mutu patshi, sikukala ndi nsaru za lini, koma wopindidwa pa
malo pa woka. Ndimo pomwe naloa anso wopunzira wina, 8
emwe nadza patsogolo ku mwanda, ndimo naona, namvana.
Kuti tsopano sanadziwa lemba, kuti akanauka anso kwa 9
akufa. Ndimo akupunzira namuka anso kwao. 10

11 Koma Mariya analikuima kunja pa mwanda kulira nsozi:
12 ndimo monga analikulira, nasuzumira m' mwanda; ndimo
aona anjelo awiri mwa zoyera kukala pansi, modzi kwa
mutu, ndi modzi kwa mapazi, pomwe ntembo wa Yesu
13 unagona. Ndimo anena nai', Nkazi, ulirira bwanje? Anena
nao, Tshifuka kuti anatshotsa Mwini wanga, ndimo sindidzi-
14 wa komwe anaika ie. Ndimo ntawi ananena tshotere,
natembenuka, ndimo aona Yesu kuima, ndimo sanadziwa
15 kuti anali Yesu. Yesu anena nai', Nkazi, ulirira bwanje?
ufuna ani? Ie, kuganiza anali wotshita m' munda, anena
nai', Fumu, ngati unamnyamula uko, nena ndi ine komwe
16 unamwika, ndimo didzamtshotsa. Yesu anena nai', Mariya.
Atembenuka, nanena nai' m' Tshihebere, Raboni; omwe ku
17 ti, Mpunzitsi. Yesu anena nai', Usanditosa; kuti kosu-
ntira sindikwezedwa kwa Atate: koma enda ku abali anga,
nunena nao, Dikwera ku Atatu anga ndi ku Atatu anu,
18 ndi ku Mulungu wanga ndi ku Mulungu wanu. Mariya
kwa Magadala adza nauza akupunzira, Daona Mwini; ndi
*bwanje kuti* ananena zintu zimenezi kwa ie.

19 Ndimo ntawi kunali madzulo, pa dzua limene, *dzua*
loamba la wiki, ndimo ntawi dzitseko dzinatsekedwa pomwe
akupunzira anali, tshifuka tsha kuopa kwa Ayuda, Yesu
nadza naima pakati, ndimo anena nao, Ntendere *ukale*
20 ndi inu. Ndimo ntawi nanena tshimene, nasonya awo
manja atshi ndi kundu latshi. Ndimo akupunzira nasekera,
21 ntawi anaona Mwini. Ndimo Yesu nanena nao onso, Nte-
ndere *ukale* ndi inu: monga Atate watumiza ine, inde
22 tshointsho ditumiza inu. Ndimo ntawi ananena tshimene-
tshi, napuma pa awo, ndimo anena nao, Landirani Nzimu
23 Woyera: zakwaipa za omwe muzikulululukira, zikululukiri-
dwa kwa awo; *zakwaipa* za omwe muzitsalitsa, zidzatsali-
tsidwa.

24 Koma Tomas, modzi wa kumi ndi awiri, atshedwa
25 Didimo, sanali nao ntawi Yesu nafika. Ndimo akupunzira
ena nanena nai', Taona Mwini. Koma nanena nao, Kani
didzaona m' manja atshi tshizindikilo tsha misomali, ndi-
dzaika tshala tshanga m' tshizindikilo tsha misomali,
ndidzaika dzanja langa m' kundu latshi, sindidzamvana.

26 Ndimo onso pambuiu masiku asanu ndi atatu akupunzira
atshi anali umo, ndi Tomas nao. Yesu adza, dzitseko
dzinatsekedwa, naima pakati, nati, ntendere *ukale* ndi inu.
27 Ndimo anena ndi Tomas, Turutsa tshala tshako, nuona

manja anga; nuturutsa dzanja lako, nuika m' kundu langa:
nusakala wopanda mvanu, koma kala ndi mvanu. Tomas 28
naiang'ka nanena nai', Mwini wanga ndi Mulungu wanga.
Yesu anena nai', Tshifuka waona ine, wamvana: odala *ali* 29
omwe sanaona, koma anamvana.

Ndimo zizindikilo zina zambiri Yesu natshita patsogolo pa 30
nkope za akupunzira, zomwe zosalembedwa m' buku limene:
koma zimenezi zilembedwa, monga kuti mungomvana kuti 31
Yesu ali Kristu, Mwana wa Mulungu; ndi kuti kumvana
mungokala ndi moyo m' dzina latshi.

Pambuiu zintu zimenezi Yesu nadzisonya anso ku akupu- 21
nzira pa nyanja ya Tiberiyas; ndimo tshointshi na*dzi*sonya.
Analipo Simon Petros, ndi Tomas atshedwa Didimo, ndi 2
Natanayeli kwa Kana mwa Galileya, ndi *ana* a Zebediya,
ndi awiri ena a akupunzira atshi. Simon Petros anena nao, 3
Ding'ka ku edza. Anena nai', Tidza anso nawe. Naturuka,
naloa m' tshombo; ndimo usiku womwe sanagwira kantu.
Koma ntawi kunali kutsha, Yesu naima pa doko; koma 4
akupunzira sanadziwa kuti anali Yesu. Ndimo Yesu anena 5
nao, Ana, muli ndi kantu ku dia? Anaiang'ka ie, Iai.
Nanena nao, Ponyani ukonde pa kundu lamanja la tshombo, 6
ndimo mudzapeza. Ndimo naponya, ndimo tsopano sana-
dziwa kuukoka kwa nsomba zambiri. Ndimo wopunzira 7
amene iemwe Yesu nakonda anena ndi Petros, Ali Mwini.
Ndimo ntawi Simon Petros anamva kuti anali Mwini,
namanga maraia atshi pa ie (kuti anali wamariseke),
nadziponya m' nyanja. Koma akupunzira ena nadza m' 8
katshombo (kuti sanali kutali ndi ntunda, koma kapena
mikono mazana awiri), kukoka ukonde *wodzaza* ndi nsomba.
Ndimo ntawi naturuka pa ntunda, aona moto wa makala 9
apo, ndi nsomba zinaikidwa apo, ndi mikate. Yesu anena 10
nao, Tengani za nsomba zomwe mwagwira tsopano. Ndimo 11
Simon Petros nakwera, nakoka ukonde pa ntunda, wodzaza
ndi nsomba zazikuru, makumi okaoka kumi, makumi asanu
ndi zitatu: koma kuti zinali zambiri, ukonde usanang'ambi-
kidwa. Yesu anena nao, Idzani mususule. Ndimo palibe 12
modzi wa akupunzira nadziwa kumfunsa, Uli ani? kudziwa
kuti anali Mwini. Yesu adza, natenga nkate, napatsa ku 13
awo, ndi nsomba anso. Ndimo amene ali tsopano ntawi 14
yatshitatu kuti Yesu nasonyezedwa ku akupunzira, pambuiu
pomwe nauka kwa akufa.

Ndimo ntawi anasusula, Yesu anena ndi Simon Petros, 15

Simon, *mwana* wa Yohane, kodi undifuna kopambana awa?
Anena nai', Inde, Mwini; udziwa kuti dikukonda. Anena
16 nai', Eta ana a nkosa anga. Anena nai', anso tshiwiri,
Simon, *mwana* wa Yohane, kodi undifuna? Anena nai',
Inde, Mwini; udziwa kuti dikukonda. Anena nai', Busa
17 nkosa zanga. Anena nai' tshitatu, Simon, *mwana* wa
Yohane, kodi undikonda? Petros anali ndi tshisoni tshi-
fuka nanena ndi ie tshitatu, Kodi undikonda? Ndimo
nanena nai', Mwini, udziwa zintu zonse; udziwa kuti
18 dikukonda. Yesu anena nai', Eta nkosa zanga. Dinena ndi
iwe nditu, nditu, Ntawi unali wang'ono, unamanga iwe eka,
ndi unaenda komwe unafuna: koma ntawi udzakala wakali,
udzaturutsa manja ako, ndimo wina adzakumanga, nadza-
19 kunyamula komwe usafuna. Ndimo tshimene natshinena,
kusonya ndi imfa yanje akapambanitsa Mulungu. Ndimo
20 ntawi ananena tshimene, anena nai', Tsata ine. Petros,
kutembenuka, aona wopunzira iemwe Yesu nakonda kutsata;
iemwe enso anatsamira pa tshifua patshi pa ngonero, nati,
21 Mwini, iemwe akuzonda ali ani? Ndimo Petros kumona
22 anena ndi Yesu, Mwini, nanga ameneyu? Yesu anena nai',
Ngati difuna kuti adzakala ntawi didza, nanga tshiani ku
23 iwe? tsata ine. Ndimo kunaturuka kunena kumene mwa
abali, kuti wopunzira uyu sakafa: koma Yesu sananena
nai', kuti sakafa; koma, Ngati difuna kuti adzakala ntawi
didza, nanga tshiani ku iwe?
24 Amene ali wopunzira iemwe amariza ndi zintu zimenezi,
nalemba zintu zimenezi: ndimo tidziwa kuti kumariza
kwatshi kuli kwanteradi.
25 Ndimo ziripo zintu zina zambiri zomwe Yesu nazitshita,
zomwe ngati zikalembedwa zonse, diganiza kuti inde dziko
lonse loka losadziwa ku landira mabuku omwe akalembe-
dwa.

# NTSHITO ZA APOSTILE.

1 MAU atsogolo dinapanga, O Teyofilo, ndi zonse zomwe
2 Yesu naamba ku tshita ndi ku punzitsa, ku siku
momwe analandiridwa ku mwamba, pambuiu kuti ndi Nzimu

Woyera anapatsa mau, ku apostile omwe anasang'kidwa:
kwa omwe enso nadzisonyeza ndi moyo pambuiu kumva 3
kwatshi ndi zizindikilo zambiri, kudzisonyeza ku awo kwa
masiku makumi anai, ndi kunena ndi zintu za dziko la
Mulungu: ndimo, kukomana nao, nauza awo si ku tshoka 4
ku Yerusalem, koma ku lindira kwa kulonjezana kwa Atate,
komwe, *wati*, munamva kwa ine: kuti Yohane nditu 5
nabapatiza ndi madzi; koma mudzabapatizidwa ndi Nzimu
Woyera si masiku ambiri alinkudza.

Ndimo awo, ntawi anasong'kana, namfunsa, kuti, Mwini, 6
kodi uli pa ntawi yatsopano ku bweza dziko ku Sirayeli?
Ndimo nanena nao, Sikuli kwa inu ku dziwa zintawi ndi 7
zinsiku, zomwe Atate anaikidwa mwa mpamvu yatshi. Koma 8
mudzalandira mpamvu, ntawi Nzimu Woyera unafika pa
inu: ndimo mudzakala omariza anga m' Yerusalem, ndi
mwa Yudeya lonse, ndi m' Samariya, ndi kwa kutali kwa
dziko. Ndimo ntawi nanena zintu zimenezi, monga ana- 9
likuyang'ana, anatengedwa; ndi ntambo walandira ie kwa
kuona kwao. Ndimo ntawi analikuyang'anitsa m' mwa- 10
mba monga analikupita, ona, antu awiri naima pafupi ndi
awo mwa nsaru zoyera; omwe enso nati, Amuna, Agalileya, 11
bwanje muima kuyang'ana m' mwamba? Yesu amene,
emwe analandiridwa kwa inu m' mwamba, tshointsho adza-
fika monga munaona ie ku pita m' mwamba.

Ndimo nabwera ku Yerusalem ku piri litshedwa Maolive, 12
lomwe liri pafupi ndi Yerusalem, ulendo wa dzua la sabata.
Ndimo ntawi analoa, nakwera mwa tshipinda tshamwamba, 13
pomwe analikukala; Petros ndi Yohane ndi Yakobi ndi
Andreya, Filipu ndi Tomas, Bartolemeyu ndi Mateyu, Yakobi
*mwana* wa Alifeyu, ndi Simon Mzelote, ndi Yuda *mwana*
wa Yakobi. Awo onse ndi ntima umodzi nakalabe kolimba 14
m' kupempera, ndi akazi, ndi Mariya amai *atshi* a Yesu,
ndimo ndi abali atshi.

Ndimo m' masiku amene Petros naima mkati mwa abali, 15
nati (ndimo munali antu ambiri *anasong'kanidwa*, kapena
makumi okaoka kumi, ndi makumi awiri), Amuna, abali, 16
kunali kufunidwa kuti mlemba likadzazidwa, lomwe
Nzimu Woyera unanena patsogolo mwa nkamwa mwa
Davide ndi Yuda, emwe anali wotsogolera kwa omwe
nagwira Yesu. Kuti anawereng'jedwa ndi ife, nalandira 17
kugawa kwatshi m' kuimirira kumene. (Ndimo muntu 18
amene nalandira munda ndi kulipira kwa mpulupulu yatshi;

ndimo kugwa ndi mutu patsogolo, nasweka pakati, ndimo
19 matumbo atshi onse anaturuka. Ndimo tshinadziwidwa
ku onse omwe nakala m' Yerusalem; monga kuti m' liu lao,
munda umene unatshedwa Akeldama, omwe ali, Munda
20 wa mwazi.) Kuti tshilembedwa m' buku la Masalmo,

Malo atshi apangidwe dzinja,
Ndi palibe muntu akale umo:

ndi,

Kuyang'anira kwatshi wina atenge.

21 Ndimo wa amuna omwe anapatikana ndi ife ntawi yonse
22 yomwe Mwini Yesu naloa naturuka mwa ife, kuamba kwa
mbapatisma la Yohane, ku siku lomwe analandiridwa
kumwamba kwa ife, wa amenewa modzi akanakala woma-
23 riza ndi ife wa kuukirira kwatshi. Ndimo naika awiri,
Yosefe atshedwa Barsaba, emwe nasintanitswa Yusto, ndi
24 Matiya. Ndimo napempera, nati, Iwe, Mwini, emwe
udziwa mitima ya antu onse, sonyeza wa amenewa awiri,
25 modzi emwe wasang'ka, ku tenga malo m' kuimirira kumene
ndi upostile, kwa zomwe Yuda nagwa, kuti anangomuka
26 kwatshi. Ndimo napatsira kuyesa kwa awo; ndimo kuyesa
kunagwa pa Matiya; ndimo anawereng'jedwa ndi apostile
kumi ndi modzi.

2 Ndimo ntawi siku la Pentekoste linafika, anali onse
2 pa malo modzi. Ndimo nsanga kunadzera kumwamba
namalowe monga mpepo yopita nsanga yolimba, ndimo
3 inadzaza nyumba yonse momwe analikukala. Ndimo kuna-
sonyeza ku awo malilume kugawana, monga a moto;
4 ndimo linakala pa onse pa awo. Ndimo nadzazidwa onse
ndi Nzimu Woyera, naamba ku lankula ndi malilume ena,
monga Nzimu unapatsa awo kulankula.

5 Ndimo kunali kukala pa Yerusalem Ayuda, amuna
6 opembedza, ku mitundu yonse pansi pakumwamba. Ndimo
ntawi namalowe amene anamvedwa, antu ambiri anaso-
ng'kana, nadodometsedwa, tshifuka kuti antu onse anamva
7 awo kulankula m' liu lao. Ndimo onse nazizwa nazirimu-
kwa, kuti, Ona, onse awa omwe alankula kodi si ali Agali-
8 leya? Ndimo bwanje timva, antu onse m' liu latu, m'
9 lomwe tinabadwa? Aparti ndi Amedi ndi Aelami, ndi
okala m' Mesopotamiya, m' Yudeya ndi m' Kapadokiya,
10 m' Ponto ndi m' Asiya, m' Firigiya ndi m' Pamfiliya, m'
Yiputa ndi m' malo a Libiya pa Kirene, ndi alendo kwa
11 Roma, Ayuda ndi openduka, Akirete ndi Anasara, timva

awa kulankula m' mau atu zintu zazikuru za Mulungu.
Ndimo onse nazizwa, naganizidwaganizidwa, kunena ku 12
modzi ndi wina, Tshimene tshitantauza tshiani? Koma 13
ena kunyoza nati, Adzazidwa ndi vinyo watsopano.

Koma Petros, kuima ndi kumi ndi modzi, natukula liu 14
latshi, nanena nao, *kuti*, Amuna, Ayuda, ndi onse inu nomwe
mukala m' Yerusalem, tshimene tshidziwidwa ndi inu, ndimo
imvani ndi mau anga. Kuti amene osali oledzera, monga 15
muganiza; kuti kuli *koka* ora latshitatu la dzua; koma 16
tshimene tshiri tshomwe tshanenedwa mwa mprofeti Yoweli;

Ndimo kudzali m' masiku akutungo, ati Mulungu, 17
Didzatsanula wa Nzimu wanga pa nyama zonse:
Ndimo ana amamuna anu ndi ana akazi anu adzalosa,
Ndimo anyamata anu adzaona zoona,
Ndimo antu akalamba anu adzalota maloto:
Inde ndi pa akapolo anga ndi pa adzakazi anga m' 18
masiku adya
Didzatsanula wa Nzimu wanga; ndimo adzalosa.
Ndimo didzasonyeza zozizwa m' mwamba, kumwa- 19
mba,
Ndi zizindikilo pa dziko pansi;
Mwazi, ndi moto, ndi mpwea wa utsi:
Dzua lidzatembenuzidwa ku ndima, 20
Ndi mwezi ku mwazi,
Patsogolo pa siku la Mwini lidza,
*Siku* lalikuru ndi losonyeza:
Ndimo kudzali, kuti iemwe adzaitana pa dzina la 21
Mwini adzapulumutsidwa.

Amuna, Asirayeli, imvani mau amene: Yesu wa Nazarete, 22
mamuna wosimbidwa ndi Mulungu kwa inu ndi zimpamvu
ndi zozizwa ndi zizindikilo, zomwe, Mulungu natshita ndi
ie m' kati mwa inu, inde monga mudziwa inu noka; ie, 23
kubwezedwa ndi kuweruza kotshitidwa ndi kudziwapatsogolo
kwa Mulungu, inu ndi dzanja la antu opanda mau muna-
mpatshika munampa: emwe Mulungu anaukitsa, kunama- 24
sula maululu a imfa: tshifuka kuti kusadziwa ku ta kuti
ie akagwidwa ndi iyo. Kuti Davide anena ndi ie, 25

Dinaona Mwini ntawi zonse patsogolo pa nkope yanga;
Tshifuka kuti ali pa dzanja lamanja langa, kuti
sindikasuntidwa:
Ndimo ntima wanga unali ndi tshimwemwe, ndi 26
lilume langa linasekera;

Inde ndimo nyama yanga anso idzakala m' kulingalira:
27 Tshifuka kuti sudzasia nzimu wanga m' Hadesi,
Kapena sudzapatsa Woyera wako ku ona kubvunda.
28 Unadziwitsa ine njira za moyo;
Udzadzaza ine ndi tshimwemwe ndi nkope yako.
29 Amuna, abali, dingonena ndi inu poyera ndi mbuiye wa-
ng'kuru Davide, kuti nafa naikidwa m' mwanda, ndi
30 mwanda watshi uli ndi ife ku siku limene. Ndimo ali
mprofeti, ndimo kudziwa kuti Mulungu analumbira ndi
lumbiro kwa ie, kuti wa dzobala dza mtshunu mwatshi
31 akaika *modzi* pa mpando wotshuka watshi; ie kuona patso-
golo *tshimene* nalankula ndi kuukirira kwa Kristu, kuti
sanasiidwa m' Hadesi, kapena nyama yatshi siinaona
32 kubvunda. Yesu amene, Mulungu anaukitsa, wa emwe
33 tiri onse omariza. Ndimo kunatalitsidwa ndi dzanja la-
manja la Mulungu, ndimo nalandira kwa Atate kulonjezana
kwa Nzimu Woyera, watsanula tshimene, tshomwe muona
34 ndi mumva. Kuti Davide sanakwera m' miamba: koma
anena eka,
Mwini nanena ndi Mwini wanga, Kala iwe pa dzanja
langa lamanja,
35 Kwa ntawi dipanga maliwongo ako mpando wa ma-
pazi ako.
36 Ndimo nyumba yonse ya Sirayeli idziwe nditu, kuti Mulu-
ngu wapanga ie inde Mwini ndi Kristu, Yesu amene emwe
munapatshika.
37 Ndimo ntawi anamva *tshimene*, anamyukidwa m' mitima
yao, nanena ndi Petros ndi ena a apostile, Amuna, abali,
38 tidzatshita tshiani? Ndimo Petros *nanena* nao, Tembenu-
zani mitima yanu, ndimo bapatizidwani inu nonse m' dzina
la Yesu Kristu kwa kubweza kwa zakwaipa zanu; ndimo
39 mudzalandira tshaulere tsha Nzimu Woyera. Kuti kulo-
njezana kuli kwa inu, ndi kwa ana anu, ndi kwa onse omwe
ali kutali, *inde* monga ambiri monga Mwini Mulungu watu
40 adzaitana kwa ie. Ndimo ndi mau ambiri ena namariza,
nataulira awa, kuti, Dzipulumutsani kwa fuko limene
41 lokotakota. Ndimo awa omwe analandira mau atshi,
anabapatizidwa: ndimo anaong'khetsedwa *kwa awo* m'
42 siku limene kwa mizimu mazousan atatu. Ndimo naka-
labe kolimba m' kupunzira ndi unzao za apostile, m' kuswa
kwa nkate ndi mapempero.
43 Ndimo kuopa kunafika pa mizimu yonse: ndimo zozizwa

zambiri ndi zizindikilo zinatshitidwa ndi apostile. Ndimo 44
onse omwe anamvana anali pamodzi, ndimo anapotshera
zintu zonse pamodzi; ndimo nagulitsa zintu zao ndi tshuma, 45
nazigawa kwa onse, monga antu onse anali ndi kufunidwa.
Ndimo siku ndi siku, kukalabe kolimba ndi ntima umodzi m' 46
tempile, ndi kuswa nkate kwao, anatenga kudia kwao ndi
kusekera ndi umodzi wa ntima, kulemekeza Mulungu, ndi 47
kupotshera kuanja ndi antu onse. Ndimo Mwini anao-
ng'khetsa kwa awo siku ndi siku awo omwe analikupulu-
mutsidwa.

3 Ndimo Petros ndi Yohane analikukwera ku tempile pa
ora la kupempera, *kuli ora* latshisanu ndi tshinai. Ndimo 2
muntu modzi emwe anali wopunduka miendo kwa tshibaliro
tsha amai atshi ananyamulidwa, emwe anaika masiku onse
pa tshitseko tsha tempile tshomwe tshitshedwa Tshabwino,
ku funsa tshaulere kwa awo omwe naloa m' tempile; emwe 3
aona Petros ndi Yohane afuna ku loa m' tempile, nafunsa
ku landira tshaulere. Ndimo Petros, kuyang'anitsa ie, ndi 4
Yohane, nati, Yang'ana pa ife. Ndimo anasamala awo, 5
kuganiza ku landira kantu kwa awo. Koma Petros nati, 6
Silivere ndi golide diribe; koma tshomwe diri natsho, tsho-
mwe dikupatsa. M' dzina la Yesu Kristu wa Nazarete, enda.
Ndimo namtenga ndi dzanja lamanja, namwimitsa: ndimo tso- 7
pano lino mapazi atshi ndi zimfula zatshi zinalandira mpamvu.
Ndimo kulumpa, naima, ndimo naamba ku enda; naloa nao 8
m' tempile, kuenda, ndi kulumpa, ndi kulemekeza Mulungu.
Ndimo antu onse namona kuenda ndi kulemekeza Mulungu: 9
ndimo nadziwa ndi ie, kuti anali ie emwe nakala kwa 10
zaulere pa Tshitseko Tshabwino tsha tempile: ndimo ana-
dzazidwa ndi kuzizwa ndi kuzirimuka ndi tshomwe tshina-
fika pa ie.

Ndimo monga nagwira Petros ndi Yohane, antu onse 11
natamanga pa modzi pa awo m' balanda lomwe litshedwa
la Solomon, kuzizwa kwambiri. Ndimo ntawi Petros 12
nakuona, naiang'ka ndi antu, Amuna, Asirayeli, bwanje mu-
zizwa ndi muntu amene? kapena bwanje muyang'anitsa ife,
monga ngati ndi mpamvu yatu kapena kupembedza .tina-
panga ie ku enda? Mulungu wa Abraham, ndi wa Yisake, 13
ndi wa Yakobi, Mulungu wa atatu atu, wapambanitsa
Mwana watshi Yesu, emwe munapereka, ndimo nakana
patsogolo pa nkope ya Pilato, ntawi anayerekeza kummasula.
Koma munakana Woyera ndi Wodeka, ndimo munafunsa 14

15 wambanda ku patsidwa kwa inu, ndimo munapa Woweruza
wa Moyo; emwe Mulungu anaukitsa kwa akufa; ndi emwe
16 tiri omariza. Ndimo ndi mvanu m' dzina latshi, dzina latshi
linapanga muntu amene wolimba, emwe muona ndi mudziwa:
inde, mvanu womwe uli mwa ie wapatsa ie kulimba kuta
17 kumene patsogolo pa inu nonse. Ndimo tsopano, abali, di-
dziwa kuti m' kusadziwa munakutshita, monga natshita anso
18 oweruza anu. Koma zintu zomwe Mulungu anasonyeza
patsogolo ndi nkamwa mwa aprofeti onse, zomwe Kristu
19 watshi akanamva, anadzaza tshointshi. Ndimo tembenu-
zani mitima yanu, ndimo tembenukani inso, kuti zakwaipa
zanu zingofafanizidwa, kuti tshointshi zingofika ntawi za
20 kusangalatsa kwa nkope ya Mwini; ndimo kuti angotumiza
21 Kristu emwe waikidwa kwa inu, *inde* Yesu: emwe mwa-
mba mukanalandira kwa ntawi za kubwezera kwa zintu
zonse, ndi zomwe Mulungu nalankula ndi nkamwa mwa
aprofeti atshi oyera omwe anali kwa ntawi dziko linaamba.
22 Moses nati nditu, Mwini Mulungu adzaukitsa kwa inu mpro-
feti kwa abali anu, wofana ndi ine; kwa ie mudzamvana
23 mwa zintu zonse zomwe adzalankula ndi inu. Ndimo
kudzali, kuti mizimu yonse, yomwe isadzamva ndi mprofeti
24 amene, idzamwazidwa nditu kwa antu. Inde ndi aprofeti
onse kwa Samueli ndi awo omwe anatsata, monga ambiri
monga analankula, awo onso anauza ndi masiku amene.
25 Muli ana a aprofeti, ndi a kupangana komwe Mulungu
anapanga ndi atatu anu, kunena ndi Abraham, Ndimo mwa
26 mbeu yako mabanja onse a dziko adzadalitsidwa. Kwa inu
patsogolo Mulungu, anaukitsa Mwana watshi, natumiza ie ku
dalitsa inu, m' kutembenuza inu nonse kwa mpulupulu zanu.

4 Ndimo monga nalankula ndi antu, adzukuru ndi kazembe
2 wa tempile, ndi Asadusi nadza pa awo, kutetimera kwa-
mbiri tshifuka napunzitsa antu, nauza m' Yesu kuukirira
3 kwa akufa. Ndimo naika manja pa awo, naika awo m'
nyumba ya ndima kwa mawa: kuti tsopano ali madzulo.
4 Koma ambiri a awo omwe anamva mau namvana; ndimo
kuwerenga kwa amuna kunali pa mazousan asanu.

5 Ndimo kunali pa mawa, kuti oweruza ao ndi akuru ndi
6 akulembera anasong'kanidwa m' Yerusalem; ndimo Hana
ndzukuru wang'kuru *anali apo*, ndi Kayafa, ndi Yohane, ndi
Alesandire, ndi monga ambiri monga anali a abali a ndzu-
7 kuru wang'kuru. Ndimo ntawi anaika awo m' kati, nafunsa,
Ndi mpamvu yanje, kapena m' dzina lanje, munatshita

tshimene? Ndimo Petros, anadzazidwa ndi Nzimu Woyera, 8
nanena nao, Oweruza inu a antu, ndi akuru,. ngati lero 9
limene tifunsidwa ndi ntshito yabwino yotshitidwa ku
muntu wopanda mpamvu, ndi mwa ani muntu amene atshiri-
tsidwa; tshidziwidwe kwa inu nonse, ndi ku antu onse a 10
Sirayeli, kuti m' dzina la Yesu Kristu wa Nazarete, emwe
munapatshika, emwe Mulungu anaukitsa kwa akufa, *inde* mwa
ie muntu amene aima pano watshiritswa patsogolo pa inu.
Ie ali mwala womwe unapeputsidwa ndi inu omanga, womwe 11
unapangidwa mutu wa ngondia. Ndimo m' mulibe wina kulipo 12
kupulumutsa: kuti kapena posali dzina lina pansi pa mwamba,
lomwe lipatsidwa mwa antu, m' lomwe tikanapulumutsidwa.

Tsopano ntawi naona kulimbika ntima kwa Petros ndi 13
Yohane, ndimo anadziwitsa kuti anali antu osapunzitsidwa
ndi osadziwa, nazizwa; nadziwa awo, kuti anali ndi Yesu.
Ndimo kuona muntu emwe anatshiritsidwa kuima nao, 14
osadziwa ku nena kantu pa iko. Koma ntawi anauza awo 15
ku tshoka kwa gulu la ankoswe, nauzana mwa iwo oka,
kuti, Titshita tshiani ndi antu awo? tshifuka kuti nditu 16
tshizindikilo tshodziwidwa tshatshitidwa mwa awo, tshi-
sonyezedwa kwa onse omwe akala m' Yerusalem; ndimo
sitidziwa ku tshikana. Koma kuti sitshiyanika kopambana 17
mwa antu, tiopse awo, kuti kwa ntawi imene alankule ndi
palibe muntu m' dzina limene. Ndimo naitana awo, nauza 18
awo sikunena konse kapena sikupunzitsa m' dzina la Yesu.
Koma Petros ndi Yohane naiang'ka nanena nao, Ngati 19
tshiri tshabwino m' kuona kwa Mulungu ku mva inu
kopambana Mulungu, weruzani: kuti sitidziwa koma ku 20
lankula zintu zomwe tinaona tinamva. Ndimo awa, ntawi 21
anaopsa awo kopambana, naaleka, kupeza tshabe bwanje
anangoalanga, tshifuka tsha antu; kuti antu onse napa-
mbanitsa Mulungu kwa tshimene tshomwe tshinatshitidwa.
Kuti muntu anali ndi moyo wopambana dzaka makumi 22
anai, pa emwe tshizindikilo tshimene tsha kutshiritsa tshina-
tshitidwa.

Ndimo kulekedwa, nadza ku gulu lao, nabukitsa onse 23
omwe adzukuru akuru ndi akuru ananena nao. Ndimo 24
awo, ntawi anaimva, natukula liu lao kwa Mulungu ndi
ntima umodzi, nati, O Ambuiye, iwe emwe unapanga ku-
mwamba ndi pansi ndi nyanja, ndi zonse zomwe ziri
mwa izo: emwe ndi Nzimu Woyera, *mwa* nkamwa mwa 25
atatu atu Davide mwana wako, unanena,

Bwanje Mitundu inakwia,
Ndi antu anaganiza ndi zintu zatshabe?
26 Mafumu otshuka a pansi anandandalika awo oka,
Ndi oweruza anasong'kanidwa,
Pa Mwini, ndi pa Kristu watshi:
27 kuti ndi nteradi m' mzinda umene pa Mwana wako
woyera Yesu, emwe unadzosa, ndi Herode ndi Pontiyo
Pilato, ndi Mitundu ndi antu a Sirayeli, anasong'kanidwa,
28 ku tshita tshomwe dzanja lako ndi kuweruza kwako zina-
29 limbitsa kali ku kala. Ndimo tsopano, Mwini, yang'anira
maopsa ao: ndimo patsa kwa akapolo ako ku lankula mau
30 ako ndi kulimbika konse, ntawi uturutsa dzanja lako ku
tshiritsa; ndimo kuti zizindikilo ndi zozizwa zingotshitidwa
31 mwa dzina la Mwana wako woyera Yesu. Ndimo ntawi
anapempera, malo anantentemedwa momwe anasong'kanidwa;
ndimo onse anadzazidwa ndi Nzimu Woyera, ndimo nala-
nkula mau a Mulungu ndi kulimbika.
32 Ndi antu ambiri a awo omwe anamvana anali ndi ntima
umodzi ndi nzimu umodzi: ndimo palibe modzi *wa awo*
nanena kuti kantu ka zintu zomwe napotshera kanali
33 katshi; koma anali ndi zintu zonse pa modzi. Ndimo ndi
mpamvu yeikuru apostile napatsa kumariza kwao ndi
kuukirira kwa Mwini Yesu: ndi kufatsa kwambiri kunali
34 pa awo onse. Kuti kapena sanali mwa awo wina emwe
anasoa: kuti monga ambiri monga anali opotshera a minda
kapena zinyumba nagulitsa izo, natenga mitengo ya zintu
35 zomwe zinagulitsidwa, naika iyo pa mapazi a apostile: ndimo
kugawa kunapangidwa kwa onse, kwa monga onse asaukira.
36 Ndimo Yosefe, emwe ndi apostile nasintanidwa Barnaba
(lomwe liri, kusandukidwa, Mwana wa kutintimika), Mlevi,
37 muntu wa Kipro ndi fuko, ali ndi munda, nagulitsa iwo, na-
tenga ndrama, naziika pa mapazi a apostile.
5 Koma muntu modzi atshedwa Hananiya, ndi Safira
2 nkazi watshi, nagulitsa kupotshera, ndimo nabwezera *pande*
la ntengo, nkazi watshi inso kudziwana, ndimo natenga
3 pande limodzi, naliika pa mapazi a apostile. Koma Petros
nati, Hananiya, bwanje Satana wadzaza ntima wako ku
namiza Nzimu Woyera, ndi ku bwezera *pande* la ntengo
4 wa munda? Ntawi unakala, kodi sunakala wako? ndimo
pambuiu unagulitsidwa, kodi sunali m' mpamvu yako?
Kuli bwanje kuti unaganiza tshintu tshimene m' ntima
wako? Usananamiza kwa antu, koma kwa Mulungu.

Ndimo Hananiya kumva mau amene nagwa natsirizika: 5
ndimo kuopa kwambiri kunakala pa onse omwe anamva.
Ndimo anyamata nauka nakuta ie, namnyamula kunja 6
namwika m' mwanda.

Ndimo kunali monga pambuiu pa maora atatu, ndimo 7
nkazi watshi, kusadziwa tshomwe tshinakala, naloa. Ndimo 8
Petros naiang'ka kwa ie, Uza ine ngati munagulitsa munda
kwa kutshuruka kumene. Ndimo nati, Inde, kwa kutshu-
ruka kumene. Koma Petros *nanena* kwa ie, Kuli bwanje 9
kuti munagwirizana ku yesa Nzimu wa Mwini? ona,
mapazi a awo omwe anaika m' mwanda mamuna wako ali
pa tshitseko, ndimo adzanyamula iwe kunja. Ndimo nagwa 10
nsanga pa mapazi atshi, natsirizika: ndimo anyamata naloa
napeza ie wafa, ndimo namnyamula kunja namwika m'
mwanda pa kundu la mamuna watshi. Ndimo kuopa 11
kwambiri kunafika pa eklesia lonse, ndimo pa onse omwe
anamva zintu zimenezi.

Ndimo ndi manja a apostile zizindikilo ndi zozizwa zambiri 12
zinatshitidwa mwa antu; ndimo awo onse anali ndi ntima
umodzi m' balanda la Solomon. Koma a ena palibe modzi 13
nayesa ku dzipatika ndi awo: koma antu anatshurukitsa awo; 14
ndimo amvanu anaong'khetsedwa kopambana kwa Mwini,
ambiri a antu ndi a akazi; monga kuti inde nanyamula 15
kunja odwala mu makwalala, naika awo pa akama ndi pa
akama ang'ono, kuti, monga Petros napita, inde tshitunzi
tshatshi tshinangopimba wina wa awo. Ndimo onso nasong'- 16
kana antu ambiri ku mizinda yozungulira Yerusalem, kutenga
odwala, ndi awo omwe anantentemeredwa ndi mizimu
yosatsuka: ndimo anatshiritsidwa onse.

Koma ndzukuru wang'kuru nauka, ndi onse omwe anali 17
nai' (kuli kugana kwa Asadusi), ndimo anadzazidwa ndi
nsanje, ndimo naika manja pa apostile, naika awo m' 18
nyumba ya ndima. Koma njelo wa Mwini usiku natsegula 19
zitseko za nyumba ya ndima, naaturutsa, ndimo nati,
Mukani, ndi kuima lankulani m' tempile ku antu mau onse 20
a Moyo umene. Ndimo ntawi anamva *tshimene*, naloa m' 21
tempile pa banda kutsha, napunzitsa. Koma ndzukuru
wang'kuru nadza, ndi omwe anali nai,' naitana ku song'kana
gulu la ankoswe, ndi gulu lonse la akuru la ana a Sirayeli, natu-
miza ku nyumba ya ndima monga kuti atengedwe. Koma aka- 22
zembe omwe anafika sanapeza awo m' nyumba ya ndima;
ndimo nabwera, nauza, kuti, Nyumba ya ndima tinapeza yotseka 23

ndi yolimba, ndi akudikira anaima pa dzitseko: koma ntawi
24 tinatsegula, tinapeza mulibe muntu. Ndimo ntawi kazembe
wa tempile ndi adzukuru akuru anamva mau amene,
anatetimedwa kwambiri ndi awo kwa tshiani tshimene
25 tshikakula. Ndimo nadza modzi nauza awo, Ona, amuna
omwe munaika m' nyumba ya ndima ali m' tempile kuima
26 ndi kupunzitsa antu. Ndimo kazembe wang'kuru ndi
akazembe nang'ka, natenga awo, *koma* kopanda kukakamiza;
27 kuti naopa antu, kani akaponyedwa ndi miala. Ndimo
ntawi anatenga awo, naika awo patsogolo pa gulu la
28 ankoswe. Ndimo ndzukuru wang'kuru nafunsa awo, kuti,
Tinauza inu kolimba si ku punzitsa m' dzina limene: ndimo
ona, munadzaza Yerusalem ndi kupunzitsa kwanu, ndimo
muyerekeza ku tenga mwazi wa muntu amene pa ife.
29 Koma Petros ndi apostile naiang'ka nati, Tikanamvera
30 Mulungu kopambana antu. Mulungu wa atatu atu naukitsa
31 Yesu, emwe munapa, kupatshika ie pa ntengo. Ie Mulungu
anapambanitsa ndi dzanja latshi lamanja *ku kala* Woweruza
ndi Mpulumutsi, ku patsa kutembenuza ntima kwa Sirayeli,
32 ndi kubweza kwa zakwaipa. Ndimo tiri omariza a zintu
zimenezi; ndimo *tshointsho uli* Nzimu Woyera, womwe
Mulungu wapatsa ku awo omwe amvera ie.
33 Koma awo, ntawi anamva tshimene, namyukidwa ntima,
34 nafuna ku pa awo. Koma naima modzi mwa gulu la
ankoswe, Mfarisi, atshedwa Gamaliyeli, mpunzitsi wa mau,
anapotsheredwa mwa ulemu ndi antu onse, ndimo nauza
35 ku turutsa antu ntawi yeing'ono. Ndimo nanena nao, Antu,
Asirayeli, tshenjerani inu noka monga ndi antu amene,
36 tshomwe mutofuna ku tshita. Kuti patsogolo pa masiku
amene nauka Tuda, kunena kuti ali ie eka; kwa emwe
kuwerenga kwa antu, pa mazana anai, anadzipatika: emwe
anapedwa; ndi onse, monga ambiri monga anamvera ie,
37 anabalalitsidwa, nafika kwa tshabe. Pambuiu muntu amene
nauka Yuda wa Galileya m' masiku a kulembera, nakotshera
*ena a* antu pambuiu pa ie: ie enso namwaza; ndi onse,
38 monga ambiri monga namvera ie, anabalalitsidwa. Ndimo
tsopano dinena ndi inu, Tshokani kwa antu amene, ndimo
lekani awo oka: kuti ngati kuweruza kumene kapena
39 ntshito imene ziri za antu, zidzatembenuzidwa: koma ngati
ziri za Mulungu, simudzakala ndi mpamvu ku tembenuza
awo; kani nditu mupezedwa inde ku menyana pa Mulungu.
40 Ndimo kwa ie analola: ndimo ntawi anaitana apostile kwa

awo, namenya awo, nauza awo si kulankula m' dzina la
Yesu, naleka awo. Ndimo natshoka kwa kuona kwa gulu la 41
ankoswe, kusekera kuti anawerengedwa oenera ku mva
nyozo kwa Dzina. Ndimo masiku onse, m' tempile ndimo 42
pao, sanaleka ku punzitsa ndi ku uza Yesu *monga*
Kristu.

Ndimo m' masiku amene, ntawi kuwerenga kwa 6
akupunzira kunalikupindula, kunakala kundandaula mwa
Ayuda-Agrike pa Ahebere, tshifuka kuti amasie ao anasiidwa
m' kuimirira kwa masiku onse. Ndimo kumi ndi awiri 2
anaitana antu ambiri a akupunzira ku awo, nati, Sitshiri
tshabwino kuti tikasia mau a Mulungu, ntikaimirira magome.
Ndimo yang'anirani, abali, mwa inu amuna asanu ndi 3
awiri a mbiri yabwino, odzaza ndi Nzimu ndimo ndi nzeru,
omwe tingoloeza pa ntshito imene. Koma ife tidzakalabe 4
kolimbika m' kupempera, ndi m' kuimirira kwa mau.
Ndimo mau nasekeretsa antu ambiri onse : ndimo nasang'ka 5
Stefano, mamuna wodzaza ndi mvanu ndi Nzimu Woyera,
ndi Filipu, ndi Prokoro, ndi Nikanore, ndi Timon, ndi
Paramena, ndi Nikolawo wopenduka kwa Antiyokwe :
omwe anaika patsogolo pa apostile : ndimo ntawi anapempera, 6
anaika manja ao pa awo.

Ndimo mau a Mulungu anakula ; ndimo kuwerenga kwa 7
akupunzira kunapindula m' Yerusalem kwambiri ; ndimo
gulu lalikuru la adzukuru anamvera mvanu.

Ndimo Stefano, wodzaza ndi kufatsa ndi mpamvu, 8
natshita zozizwa zazikuru ndi zizindikilo mwa antu. Koma 9
nauka ena a awo omwe anali a sinagoge litshedwa
*sinagoge* la Amfulu, ndi la Akirene, ndi la Alesandiriya, ndi
la awo kwa Kilikiya ndi Asiya, kugazana ndi Stefano. Ndimo 10
sanali ndi mpamvu ku ima pa nzeru ndi pa Nzimu ndi
zomwe nalankula. Ndimo nanyenjera antu, omwe nanena, 11
Tamva ie kulankula mau akutukwana pa Moses, ndi
*pa* Mulungu. Ndimo nafulumiza antu, ndi akuru, ndi 12
akulembera, ndimo nadza pa ie, namgwira, namtenga kwa
gulu la ankoswe, naika omariza onama, omwe nanena, 13
Muntu amene wosaleka kulankula mau pa malo oyera
amene, ndi *pa* mau : kuti tamva ie ku nena, kuti Yesu 14
amene wa Nazarete adzamwaza malo amene, ndimo adzasintana
makalidwe omwe Moses anapereka kwa ife. Ndimo onse 15
omwe anakala m' gulu la ankoswe, kuyang'anitsa ie, naona
nkope yatshi monga inali nkope ya njelo.

7 Ndimo ndzukuru wang'kuru nati, Kodi zintu zimene
2 ziri tshointsho? Ndimo nati,
Amuna, abali, ndi atate, mumve. Mulungu wa kupambana
nadzisonya kwa atatu atu Abraham, ntawi anali m'
3 Mesopotamiya, patsogolo nakala m' Karane, nanena nai',
Tshoka dziko lako, ndi kwa abali ako, nudza m' dziko lomwe
4 didzasonyeza iwe. Pomwe natshoka kwa dziko la Akaldi,
ndimo nakala m' Karane: ndi kwa uko, ntawi atatu atshi
anafa, *Mulungu* nasunta ie m' dziko limene, momwe mukala
5 tsopano: ndimo sanampatsa kuloa mwa ilo, iai, sitshuruka
monga ku ika pazi latshi pa iko: ndimo nalonjezana kuti
akakupatsa kwa ie m' kupotshera, ndi kwa mbeu yatshi
6 pambuiu pa ie, ntawi *pomwe* sanapotshera mwana. Ndimo
Mulungu nalankula tshointshi, kuti mbeu yatshi ikakala
alendo m' dziko lina, ndi kuti akatenga iyo mumpawi,
7 nakatshita nkarwe naiyo, dzaka mazana anai. Ndimo
mtundu kwa womwe idzakala mumpawi didzaweruza, nati
Mulungu: ndimo pambuiu pa kumene idzaturuka, ndimo
8 idzaimirira ine m' malo amene. Ndimo napatsa ie kupa-
ngana kwa kudula: ndimo tshointsho *Abraham* nabala
Yisake, nadula ie pa siku latshisanu ndi tshitatu; ndimo
Yisake *nabala* Yakobi, ndi Yakobi ambuiye akuru kumi ndi
9 awiri. Ndimo ambuiye akuru, anasukunyidwa ndi nsanje
10 pa Yosefe, nagulitsa ie kwa Yiputa: ndimo Mulungu anali
nai', namtshotsa kwa masautso atshi onse, nampatsa kuanja
ndi nzeru patsogolo pa Faro fumu yotshuka ya Yiputa;
ndimo nampanga woweruza pamwamba pa Yiputa ndi pa
11 nyumba yatshi yonse. Ndimo inadza njala pa Yiputa lonse
ndi Kanane, ndi sautso yeikuru: ndimo atatu atu sanapeza
12 kantu ku dia. Koma ntawi Yakobi anamva kuti dzinali
13 dzintu m' Yiputa, natumiza atatu atu ntawi yoamba. Ndimo
pa ntawi yatshiwiri Yosefe nadziwidwa ku abali atshi; ndimo
14 fuko la Yosefe linasonyezedwa kwa Faro. Ndimo Yosefe natu-
miza, naitana kwa ie atatu atshi Yakobi, ndi abali atshi onse,
15 mizimu makumi atatu ndi kumi ndi isanu. Ndimo Yakobi
natsika kwa Yiputa; ndimo nafa, ie eka, ndi atatu atu;
16 ndimo nanyamulidwa kwa Shekem, naikidwa m' mwanda
womwe Abraham nagula kwa ntengo m' silivere kwa ana a
17 Hamore m' Shekem. Koma monga ntawi ya kulonjezana
inayandika, komwe Mulungu napatsa ku Abraham, antu
18 nakula napindula m' Yiputa, kwa ntawi inauka fumu
yotshuka ina pa mwamba pa Yiputa, yomwe isanadziwa

Yosefe. Yomwe inatshita kotshenjera ndi fuko latu, ndimo 19
inatshita nkarwe ndi atatu atu, kuti akaturutsa tiana tao
monga kuti tisanangokala ndi moyo. Pa nsiku imene Moses 20
anabadwa, ndimo anali wabwino wopambana, kwa Mulungu;
ndimo naleredwa m' nyumba ya atatu atshi miezi itatu:
ndimo ntawi anaturutsidwa, mwana wankazi wa Faro 21
namtenga, namlera monga mwana watshi. Ndimo Moses 22
anapunzitsidwa m' nzeru zonse za Ayiputa; ndimo anali
wolimba m' mau atshi ndi ntshito *zatshi.* Koma ntawi 23
anali moyo pafupi ndi dzaka makumi anai, tshinaloa m'
ntima watshi ku tsheza ndi abali atshi ana a Sirayeli.
Ndimo kuona modzi *wa awo* kumva kwaipa, namtontoza, 24
namulira ie emwe anasautsidwa, kumenya Myiputa:
ndimo naganizaganiza kuti abali atshi nadziwa bwanje 25
kuti Mulungu ndi dzanja latshi analikupatsa awo kupulu-
mutsa; koma sanadziwa. Ndimo siku kutsala nadzisonya kwa 26
awo monga anatetana, nafuna ku anjanitsa awo anso, kuti,
Mafumu, muli abali; bwanje mutshimwana? Koma iemwe 27
anatshimwa ndi woiandikila watshi namtshotsa, kuti,
Ndani napanga iwe fumu ndi woweruza pa ife? Kodi 28
ufuna kundipa, monga unapa Myiputa dzulo? Ndimo 29
Moses natawa pa mau amene, nakala waulendo m' dziko
la Midyan, pomwe nabala ana awiri. Ndimo ntawi dzaka 30
makumi anai dzinadzazidwa, njelo nadzisonyeza kwa ie m'
tshipululu tsha piri la Sinai, m' lilume la moto m' tshifutu.
Ndimo ntawi Moses natshiona, nazizwa pa kuona: ndimo 31
monga nayandika ku ona, linadza liu la Mwini, Diri 32
Mulungu wa atatu ako, Mulungu wa Abraham, ndi wa
Yisake, ndi wa Yakobi. Ndimo Moses nantuntumira,
ndimo sanayesa ku ona. Ndimo Mwini nanena nai', Masula 33
dzikwakwata kwa mapazi ako: kuti malo pomwe uima
iri ntaka yoyera. Dinaona nditu sautso ya antu anga 34
omwe ali m' Yiputa, ndimo dinamva kubulira kwao, ndimo
datsika ku pulumutsa awo: ndimo tsopano idza, didzatumiza
iwe m' Yiputa. Moses amene emwe nakana, kuti, Ndani 35
anapanga iwe fumu ndi woweruza? iemwe Mulungu watu-
miza *ku kala* fumu ndi mombolo ndi dzanja la njelo emwe
nadzisonyeza kwa ie m' tshifutu. Muntu amene natsogoza 36
awo, kunatshita zozizwa ndi zizindikilo m' Yiputa, ndimo m'
nyanja Yofira, ndimo m' tshipululu dzaka makumi anai.
Amene ali Moses udya, emwe nanena ndi ana a Sirayeli, 37
Mprofeti Mulungu adzaukitsa kwa inu mwa abali anu,

38 wofana ndi ine. Amene ali iemwe anali m' eklesia m'
tshipululu ndi njelo emwe nalankula ndi ie m' piri la Sinai,
ndimo ndi atatu atu: emwe nalandira mau a Mulungu
39 amoyo ku patsa kwa ife: kwa emwe atatu atu sanafuna ku
mvera, koma namkana kwa awo, nabweza m' mitima yao ku
40 Yiputa, kunena ndi Haron, Panga ife milungu yomwe
idzapita patsogolo pa ife: kuti monga kwa Moses amene,
emwe natsogoza ife kwa dziko la Yiputa, sitidziwa tshomwe
41 tshinakala ndi ie. Ndimo napanga mwana wa ng'ombe m'
masiku adya, natenga nsembe kwa fano, nasekera m' ntshito
42 za manja ao. Koma Mulungu natembenuka, napereka awo
ku imirira miko ya kumwamba; monga alembedwa m' buku
la aprofeti,

Kodi munatsira kwa ine nyama zopedwa ndi zinsembe
Dzaka makumi anai m' tshipululu, O nyumba ya Sirayeli?
43 Ndimo munatenga msasa wa Moloki,
Ndimo nyenyezi ya mulungu Refan,
Masonyezo omwe munapanga ku pembedza awo:
Ndimo didzanyamula inu patsidia lina la Babilon.

44 Atatu atu anali ndi msasa wa kumariza m' tshipululu, inde
monga nasonyeza emwe nalankula ndi Moses, kuti akau-
45 panga kwa kufaniza komwe ie anaona. Womwe enso atatu
atu, m' kusintana kwao, naloetsa ndi Yoshuwa ntawi analoa
pa zintu za mitundu, yomwe Mulungu naturutsa patsogolo
46 pa nkope ya atatu atu, kwa masiku a Davide; emwe
anapeza kuanja m' kuona kwa Mulungu, nafunsa ku peza
47 malo kwa Mulungu wa Yakobi. Koma Solomon namanga
48 nyumba kwa ie. Koma Wopambana-onse wosakala m'
*nyumba* zopangidwa ndi manja; monga anena mprofeti,

49 Mwamba uli mpando wotshuka wanga,
Ndi dziko mpando wa mapazi anga:
Nyumba yanje mudzamanga kwa ine? ati Mwini:
Kapena malo anje ali *malo* a kupuma kwanga?
50 Kodi dzanja langa silinapanga zintu zonse zimene?

51 Akuumirira nkosi inu ndi osadulidwa mutima ndi m'
makutu, ntawi yonse mukaniza Nzimu Woyera: monga
52 atatu anu anatshita, tshointsho mutshita. Uti wa aprofeti
atatu anu asanazunza? ndimo napa awo omwe anasonyeza
patsogolo ndi kudza kwa Wodeka; wa emwe tsopano
53 munakala zinzondi ndi zimbanda; inu nomwe muna-

landira mau monga analimbikidwa ndi anjelo, ndimo
musanaasunga.
Ndimo ntawi anamva zintu zimenezi, anamyukidwa mitima 54
yao, ndimo nakukuta pa ie ndi mano ao. Koma ie, 55
kudzaza ndi Nzimu Woyera, nayang'anitsa m' mwamba,
naona kupambana kwa Mulungu, ndi Yesu kuima pa dzanja
lamanja la Mulungu, nati, Ona, diona miamba yotsegulidwa, 56
ndi Mwana wa muntu kuima pa dzanja lamanja la
Mulungu. Koma napfula ndi liu lalikuru, natseka makutu 57
ao, natamanga pa ie ndi ntima umodzi; ndimo namturutsa 58
muzinda, naponya miala ie: ndimo omariza naika miinjiro
yao pa mapazi a nyamata atshedwa Saulos. Ndimo naponya 59
miala Stefano, kuitana pa *Mwini*, ndi kuti, Mwini Yesu,
landira nzimu wanga. Ndimo nagwada, napfula ndi liu 60
lalikuru, Mwini, usaike mpulupulu imene pa awo. Ndimo
ntawi ananena tshimene, nagona. Ndimo Saulos anali- 8
kubvomera ndi imfa yatshi.

Ndimo linauka pa siku limene zunzo lalikuru pa eklesia
lomwe linali m' Yerusalem; ndimo onse anabalalika mwa
malo onse a Yudeya ndi Samariya, kani apostile. Ndimo 2
antu opembedza naika Stefano m' mwanda, napanga maliro
ambiri pa ie. Koma Saulos namwaza eklesia, kuloa m' 3
nyumba zonse, ndimo kugwira antu ndi akazi naika awo m'
nyumba ya ndima.

Ndimo awo omwe anabalalika naendaenda kuuza mau. 4
Ndimo Filipu natsika ku mzinda wa Samariya, nauza kwa 5
awo Kristu. Ndimo antu ambiri nasamala ndi ntima 6
umodzi kwa zintu zomwe zinanenedwa ndi Filipu, ntawi
anamva, naona zizindikilo zomwe nazitshita. Kuti *kwa* 7
ambiri a awo omwe anali ndi mizimu yosatsuka, inaturuka,
kupfula ndi liu lalikuru: ndimo ambiri omwe ananjenje-
meredwa, ndi omwe anali opunduka miendo, anatshiri-
tsidwa. Ndimo tshinali tshimwemwe tshambiri muzinda 8
umene.

Koma anali muntu modzi, dzina latshi Simon, emwe ntawi 9
yapatsogolo muzinda natshita umabisalira, nazizwitsa antu a
Samariya, kunena kuti ie eka anali modzi wang'kuru: kwa 10
emwe onse anasamala, kwa wang'ono wopambana ku
wang'kuru wopambana, kuti, Muntu amene ali mpamvu
imene ya Mulungu yomwe itshedwa Yeikuru. Ndimo 11
nasamala ie, tshifuka kuti kwa ntawi yeitali anazizwitsa awo
ndi amabisalira atshi. Koma ntawi anamvana Filipu ku- 12

uza makalidwe abwino ndi dziko la Mulungu ndi dzina la
13 Yesu Kristu, anabapatizidwa, antu ndi akazi. Ndimo Simon
onso namvana ie eka: ndimo kubapatizidwa, nakalabe ndi
Filipu; ndi kuona zizindikilo ndi mpamvu zazikuru
zinatshitidwa, nazizwitswa.
14 Ndimo ntawi apostile omwe anali pa Yerusalem anamva
kuti Samariya analandira mau a Mulungu, anatumiza kwa
15 awo Petros ndi Yohane: omwe, ntawi anatsika, napempera
16 kwa awo, kuti anangolandira Nzimu Woyera: kuti monga
yatsopano unagwa pa palibe modzi wa awo: koma
17 anabapatizidwa koka m' dzina la Mwini Yesu. Ndimo naika
18 manja ao pa awo, ndimo nalandira Nzimu Woyera. Ndimo
ntawi Simon naona kuti mwa kuika kwa manja a apostile
19 Nzimu Woyera unapatsidwa, nasonyeza awo ndrama, kuti,
Patsa ine enso mpamvu imene, kuti pa emwe diika manja
20 anga, angolandira Nzimu Woyera. Koma Petros nanena
ndi ie, Silivere lako limwaza iwe, tshifuka unaganiza ku
21 landira tshaulere tsha Mulungu ndi ndrama. Uli ndi palibe
pande kapena malo m' mau amene: kuti ntima wako suli
22 wabwino patsogolo pa Mulungu. Ndimo tembenuza ntima
wako kwa tshimene mpulupulu yako, nupempera Mwini,
ngati kapena ganizo la ntima wako lidzakululukiridwa iwe.
23 Kuti diona kuti uli m' nyongo ya kuawa ndi m' tshomangira
24 tsha mpulupulu. Ndimo Simon naiang'ka nati, Pemperani
Mwini kwa ine, kuti palibe tshimodzi tsha zintu zomwe
munanena tshifika pa ine.
25 Ndimo awo, ntawi anamariza nalankula mau a Mwini,
nabwera ku Yerusalem, nauza ivangeli ku midzi yambiri
ya Asamariya.
26 Koma njelo wa Mwini nalankula ndi Filipu, kunena,
Uka, numuka ku mwela kwa njira yomwe itsikira kwa
27 Yerusalem ku Gaza: yomwe iri tshipululu. Ndimo nauka
namuka: ndimo ona, muntu wa Tiyopiya, mfule wa
mpamvu yeikuru pansi pa Kandase, fumuyeikazi yotshuka ya
Atiyopiya, emwe anali pamwamba pa zolemera zatshi zonse,
28 emwe anadza ku Yerusalem ku pembedza; ndimo analiku-
bwera nalikukala m' tshariote latshi, ndi analikuwerenga
29 mprofeti Yesaya. Ndimo Nzimu unanena ndi Filipu,
30 Yandika, nudzipatika ku tshariote limene. Ndimo Filipu
natamanga kwa ie, namva ie kuwerenga Yesaya mprofeti,
31 nati, Kodi udziwitsa tshomwe uwerenga? Ndimo nati,
Didziwa bwanje, kani modzi adzanditsogoza? Ndimo

napempa Filipu ku kwera ndi ku kala ndi ie. Ndimo malo 32
a lemba omwe analikuwerenga anali amene,

Anatsogozwa monga nkosa kwa kupa;
Ndimo monga mwana wa nkosa patsogolo pa wometa
watshi ali wosadziwa ku lankula,
Tshointsho wosatsegula nkamwa mwatshi:
M' kutshepetsa kwatshi kuweruza kwatshi kunatshotse- 33
dwa:
Fuko latshi ndani adzaliuza?
Kuti moyo watshi utshotsedwa kwa dziko.

Ndimo mfule unaiang'ka Filipu, nati, Dipempa iwe, wa 34
ani mprofeti anena amene? wa ie eka, kapena wa wina?
Ndimo Filipu natsegula nkamwa mwatshi, ndimo kuamba 35
kwa lemba limene, nauza kwa ie Yesu. Ndimo monga 36
napita pa njira, nafika pa madzi; ndimo mfule uti, Ona,
*alipo* madzi; tshiletsa ine tshiani ku bapatizidwa? Ndimo 38
nauza tshariote ku ima: ndimo awa awiri natsika m' madzi,
Filipu ndi mfule; ndimo anabapatiza iwo. Ndimo ntawi 39
naturuka ku madzi, Nzimu wa Mwini unatshotsa Filipu;
ndimo mfule usanaona ie palibe ntawi ina, kuti unamuka
njira yatshi kusekera. Koma Filipu anapezedwa pa Azoto: 40
ndimo kupita nauza ivangeli kwa mizinda yonse, kwa ntawi
nafika kwa Kesareya.

Koma Saulos, kosuntira kupuma malimbiko ndi kupa pa 9
akupunzira a Mwini, namuka kwa ndzukuru wang'kuru,
nafunsa kwa ie maepistola ku Damasko kwa masinagoge, 2
kuti ngati anangopeza ena omwe anali a Njira, kapena
amuna kapena akazi, anangotenga awo omangidwa ku
Yerusalem. Ndimo monga naenda ulendo, nakala kuti 3
nayandika Damasko: ndimo nsanga kunawala kozunguniza
ie kuunika kwa kumwamba: ndimo nagwa pansi, namva 4
liu kunena ndi ie, Saulos, Saulos, bwanje uzunza ine?
Ndimo nati, Uli ani, Mwini? Ndimo *nati*, Diri Yesu emwe 5
uzunza: koma uka, nuloa muzinda, ndimo tshidzauzidwa iwe 6
tshomwe ukanatshita. Ndimo antu omwe anaenda ulendo 7
ndi ie naima osalankula, kumva liu, koma kusaona muntu.
Ndimo Saulos nauka kwa pansi; ndimo ntawi maso atshi 8
anatsegulidwa, sanaona kantu; ndimo natsogoza ie ndi
dzanja, namtenga m' Damasko. Ndimo anali masiku atatu 9
wopanda kuona, ndi kapena wosadia kapena wosamwa.

Ndimo kunali wopunzira modzi pa Damasko, atshedwa 10
Hananiya; ndi Mwini nanena ndi ie m' tshoona, Hananiya.

11 Ndimo nati, Ona, Di*ri pano*, Mwini. Ndimo Mwini *nanena*
nai', Uka, numuka kwa kwalala lomwe litshedwa Lolu-
ngama, nufunsa m' nyumba ya Yuda kwa modzi atshedwa
12 Saulos, muntu wa Tarso: kuti ona, alikupempera; ndimo
waona muntu atshedwa Hananiya analikuloa, ndimo kuika
manja atshi pa ie, kuti anangolandira kuona kwatshi.
13 Koma Hananiya naiang'ka, Mwini, Damva kwa *antu* ambiri
ndi muntu amene, bwanje kutshuruka mpulupulu natshita
14 kwa oyera ako pa Yerusalem: ndi pano akala ndi mpamvu
kwa adzukuru akuru ku manga onse omwe aitana pa dzina
15 lako. Koma Mwini nanena nai', Muka: kuti ali tshiwira
tshosang'ka kwa ine, ku tenga dzina langa patsogolo pa
16 Mitundu ndi mafumu otshuka, ndi ana a Sirayeli: kuti
didzasonya ie bwanje zintu zambiri akanamva kwa dzina
17 langa. Ndimo Hananiya natshoka, naloa m' nyumba;
ndimo kuika manja atshi pa ie nati, Mbali Saulos, Mwini,
*inde* Yesu, emwe anaonekera kwa iwe m' njira yomwe
unafikira, wanditumiza, kuti ungolandira kuona kwako,
18 ndimo ungodzazidwa ndi Nzimu Woyera. Ndimo tsopano
lino anagwa kwa maso atshi monga ngati anali mamba,
ndimo nalandira kuona kwatshi; ndimo nauka nabapati-
19 zidwa; ndimo nadia nalimbikitsidwa.
Ndimo anali masiku ena ndi akupunzira omwe anali pa
20 Damasko. Ndimo tsopano lino m' masinagoge nauza Yesu,
21 kuti ali Mwana wa Mulungu. Ndimo onse omwe anamva
ie anazizwa, nati, Kodi amene siali ie emwe m' Yerusalem
namwaza awo omwe anaitana pa dzina limene? ndimo
anafika kuno kwa kuyerekeza kumene, kuti anangotenga
22 awo omangidwa patsogolo pa adzukuru akuru. Koma
Saulos nakula kopambana m' mpamvu, nadodometsa Ayuda
omwe anakala pa Damasko, kulunjikiza kuti amene ali
Kristu.
23 Ndimo ntawi masiku ambiri anadzazidwa, Ayuda nagazi-
24 tsana ku pa ie: koma kunje lao linadziwidwa ku Saulos.
Ndimo nadikira dzipata anso usana ndi usiku kuti anangopa
25 ie: koma akupunzira atshi natenga ie usiku, natsitsa ie mwa
koma, kutsitsa ie muntanga.
26 Ndimo ntawi anafika ku Yerusalem, nayesa ku dzipatika
ku akupunzira: ndi awo onse naopa ie, kusamvana kuti
27 anali wopunzira. Koma Barnaba namtenga, namtsogoza
kwa apostile, nauza kwa awo bwanje anaona Mwini m'
njira, ndi kuti analankula nai', ndi bwanje pa Damasko ana

uza kolimba m' dzina la Yesu. Ndimo anali nao kuloa ndi 28
kuturuka pa Yerusalem, kuuza kolimba m' dzina la Mwini: 29
ndimo nalankula nakangana pa Ayuda-Agrike; koma
naendaenda ku pa ie. Ndimo ntawi abali nadziwa, natsitsa 30
ie ku Kesareya, ndimo namtumiza kwa Tarso.

Ndimo eklesia mwa Yudeya lonse ndi Galileya ndi 31
Samariya linali ndi ntendere, kumangidwa; ndimo, kuenda
m' kuopa kwa Mwini ndi m' kusangalatsa kwa Nzimu
Woyera, linapindulidwa.

Ndimo kunali, monga Petros napita mwa mapande onse, 32
natsika anso ku oyera omwe nakala pa Lida. Ndimo apo 33
napeza muntu modzi atshedwa Eneya, emwe anakala m'
kama watshi dzaka dzisanu ndi dzitatu; kuti ananjenjeme-
redwa. Ndimo Petros nanena nai', Eneya, Yesu Kristu 34
atshiritsa iwe: uka, yala mpasa yako. Ndimo tsopano lino
nauka. Ndimo onse omwe nakala pa Lida ndi m' Saron 35
namona, natembenuka kwa Mwini.

Ndimo kunali pa Yopa wopunzira modzi atshedwa Tabita, 36
lomwe kusandukidwa litshedwa Nswala: nkazi amene
anadzaza ndi ntshito zabwino ndi zaulere zomwe anazitshita.
Ndimo kunali m' masiku adya, kuti anadwala, nafa: ndimo 37
ntawi anasambitsa ie, naika ie m' tshipinda tsha pamwamba.
Ndimo monga Lida linali pafupi ndi Yopa, akupunzira, 38
kumva kuti Petros anali apo, natumiza amuna awiri kwa ie,
kupempa ie, Usatshedwa ku fika kwa ife. Ndimo Petros 39
nauka namuka nao. Ndimo ntawi anafika, namtenga mwa
tshipinda tshapamwamba: ndimo amasie onse naima pafupi
ie kulira misozi, ndi kusonyeza maraia ndi miinjiro zomwe
Nswala napanga, ntawi nakala nao. Koma Petros naturutsa 40
awo onse, nagwada, napempera; ndimo kutembenuka ku
ntembo, nati, Tabita, uka. Ndimo natsegula maso atshi;
ndimo ntawi naona Petros, nagalamuka. Ndimo nampatsa 41
dzanja latshi, naukitsa ie; ndimo kuitana oyera ndi amasie,
namwika patsogolo ndi moyo. Ndimo kunadziwidwa mwa 42
Yopa wonse: ndi ambiri namvana pa Mwini. Ndimo 43
kunali, kuti nakala masiku ambiri m' Yopa ndi modzi
Simon wofufuta dzikopa.

Ndimo *kunali* muntu modzi m' Kesareya, dzina latshi 10
linali Korneliyo, kenturione wa gulu litshedwa gulu la Yitaliya,
muntu wopembedza, ndi modzi emwe naopa Mulungu ndi 2
nyumba yatshi yonse, emwe napatsa zaulere zambiri kwa
antu, napempera Mulungu ntawi yonse. Naona m' tshoona 3

poyera, monga linali pa ora latshisanu ndi tshinai la dzua,
njelo wa Mulungu kuloa kwa ie, ndi kunena nai', Korneliyo.
4 Ndimo ie, kuyang'anitsa ie, ndi kuopsedwa, nati, Tshiri
tshiani, Mwini? Ndimo nanena nai', Mapempero ako ndi
zaulere zako zinakwera kwa kumbutsa patsogolo pa
5 Mulungu. Ndimo tsopano tumiza amuna ku Yopa, ndimo
6 tenga modzi Simon, emwe asintanidwa Petros: akala ndi
modzi Simon wofufuta dzikopa, nyumba ya emwe iri mbali
7 mwa nyanja. Ndimo ntawi njelo emwe nalankula nai'
anamuka, naitana awiri a abandazi atshi, ndi wankhondo
wopembedza wa awo omwe anaimirira ie ntawi yonse;
8 ndimo nauza awo zintu zonse, natumiza awo ku Yopa.
9 Ndimo pa mawa, monga anali pa ulendo wao, ndimo
nayandika mzinda, Petros nakwera pamwamba pa nyumba
10 ku pempera, pa ora latshisanu ndi tshimodzi: ndimo njala
inadza, nafuna ku dia: koma ntawi analikukonza, nagwa
11 m' tshoona; ndimo aona mwamba motsegula, ndi tshiwira
tshimodzi kutsika, monga tshinali tshopfunda tshatshikuru,
12 tshitsitsidwa ndi dzipe dzinai pa dziko: mwa kuti inali
mitundu yonse ya nyama za mapazi anai ndi zokwawa za
13 pansi ndi mbalame za mwamba. Ndimo linafika liu kwa ie,
14 Uka, Petros; ipa nudia. Koma Petros nati, Si tshointsho,
Mwini; kuti sindadia palibe ntawi kantu kena komwe kali
15 kanko kapena kosatsuka. Ndimo liu *linafika* kwa ie enso
ntawi yatshiwiri, Tshomwe Mulungu watsuka, usapanga nko.
16 Ndimo tshimene tshinatshitidwa tshitatu: ndimo tsopano
lino tshiwira tshinalandiridwa m' mwamba.
17 Ndimo monga Petros anasing'kasing'ka mwa ie eka tshiani
tshoona tshomwe anatshiona tshinangotantauza, ona, antu
omwe anatumidwa ndi Korneliyo, anafunsa kwa nyumba ya
18 Simon, naima patsogolo pa tshipata, naitana nafunsa ngati
Simon, emwe nasintanidwa Petros, analikukala umo.
19 Ndimo monga Petros naganiza pa tshoona, Nzimu unanena
20 nai', Ona, amuna atatu afuna iwe. Koma uka, nutsika,
numuka nao, usaganizaganiza kantu: kuti datumiza awo.
21 Ndimo Petros natsika kwa amuna, nati, Ona, diri ie emwe
22 mufuna: tshifukwa tshiri tshiani bwanje mwadza? Ndimo
nati, Korneliyo kenturione, muntu wodeka ndi modzi emwe
aopa Mulungu, ndimo nabukitsidwa bwino ndi mtundu
wonse wa Ayuda, anantshenjezedwa *kwa Mulungu* ndi njelo
woyera ku tumiza kwa iwe m' nyumba yatshi, ndi ku mva
23 mau kwa iwe. Ndimo naloeza awo, nakalitsa awo.

Ndimo pa mawa nauka naturuka nao, ndi ena a abali
kwa Yopa natsagana nai'. Ndimo pa mawa naloa m' 24
Kesareya. Ndimo Korneliyo analikulindira awo, anasong'-
kanitsa abali atshi ndi mabwenzi atshi a pafupi. Ndimo ntawi 25
kunali kuti Petros naloa, Korneliyo nakomana nai', nagwa
pa mapazi atshi, nampembedza. Koma Petros namukitsa, 26
kuti, Ima; Ine ndeka anso diri muntu. Ndimo monga 27
nalankula nai', naloa, ndimo apeza ambiri anasong'kanitswa:
ndimo nanena nao, Mudziwa inu noka bwanje kuti tshiri 28
tshintu si tshamau kwa muntu emwe ali Myuda ku dzipa-
tika kapena ku fika ku modzi wa mtundu wina; ndimo kwa
ine Mulungu wasonya kuti sindikanatsha muntu modzi
wanko kapena wosatsuka: mwa kuti inso dinafika wopanda 29
kukana, ntawi dinatumizidwa. Ndimo difunsa ndi kuyere-
keza kwanje munatumiza kwa ine. Ndimo Korneliyo nati, 30
Masiku anai apita, kwa ora limene, dinalikusunga ora la-
tshisanu ndi tshinai la kupempera m' nyumba yanga; ndimo
ona, muntu naima patsogolo pa ine m' nsaru zowala, ndimo 31
ati, Korneliyo, mpempero lako limvetsedwa, ndi zaulere
zako zinakumbutsidwa m' kuona kwa Mulungu. Ndimo 32
tumiza kwa Yopa, nuitana kwa iwe Simon, emwe asinta-
nidwa Petros; akala m' nyumba ya Simon wofufuta dzikopa,
mbali mwa nyanja. Ndimo tsopano lino dinatumiza kwa 33
iwe; ndimo unatshita bwino kuti wafika. Ndimo tsopano
tiri tonse muno m' kuona kwa Mulungu, kumva zintu zonse
zomwe zinauzidwa kwa iwe ndi Mwini. Ndimo Petros 34
natsegula nkamwa mwatshi, nati,

Ndi nteradi didziwitsa kuti Mulungu alibe watsang'ko:
koma m' mitundu yonse iemwe aopa ie, natshita kudeka, ali 35
wosekera kwa ie. Mau omwe natumiza kwa ana a Sirayeli, 36
kuuza makalidwe abwino a ntendere ndi Yesu Kristu (ali
Mwini wa onse)—mau amene mudziwa inu noka, omwe 37
analimbikitsidwa mwa Yudeya lonse, kuiamba kwa Galileya,
pambuiu mbapatisma lomwe Yohane nauza; *inde* Yesu wa 38
Nazarete, bwanje kuti Mulungu anadzosa ie ndi Nzimu
Woyera ndimo ndi mpamvu: emwe naendaenda kutshita
ubwino, ndi kutshiritsa onse omwe anasautsidwa ndi diabolos;
kuti Mulungu anali ndi ie. Ndimo tiri omariza a zintu 39
zonse zomwe nazitshita m' dziko la Ayuda, ndi m'
Yerusalem; emwe enso napa, kupatshika ie pa ntengo. Ie 40
Mulungu naukitsa pa dzua latshitatu, napatsa ie ku sonye-
zedwa, si kwa antu onse, koma kwa omariza emwe anasang'- 41

kidwa patsogolo ndi Mulungu, *inde* kwa ife, tomwe tinadia
42 ndi ku mwa ndi ie pambuiu anauka kwa akufa. Ndimo
nauza ife ku uza kwa antu, ndimo ku mariza kuti amene
ali iemwe aloezedwa ndi Mulungu *ku kala* Woweruza wa
43 amoyo ndi akufa. Kwa ie aprofeti onse amariza, kuti mwa
dzina latshi onse omwe amvana ndi ie adzalandira kubweza
kwa zimpulupulu.
44 Ntawi Petros analikulankula mau amene, Nzimu Woyera
45 unagwa pa awo onse omwe anamva mau. Ndimo awo a
kudula omwe anamvana nazizwa, monga ambiri monga
nadza ndi Petros, tshifuka kuti pa Mitundu unso tshinatsanu-
46 lidwa tshaulere tsha Nzimu Woyera. Kuti anamva awo
kulankula ndi malilume, ndi kupambanitsa Mulungu.
47 Ndimo Petros naiang'ka, Kodi muntu modzi adziwa ku kana
madzi, kuti amene sakanabapatizidwa, omwe analandira
48 Nzimu Woyera monga ife? Ndimo nauza awo ku bapatizi-
dwa m' dzina la Yesu Kristu. Ndimo napempa ie ku kala
masiku owereng'jeka.
11 Ndimo apostile ndi abali omwe anali m' Yudeya anamva
2 kuti Mitundu unso inalandira mau a Mulungu. Ndimo
ntawi Petros anakwera ku Yerusalem, awo omwe anali a
3 kudula nakangana ndi ie, kuti, Unaloa ndi antu osadulidwa,
4 ndimo unadia nao. Koma Petros naamba, nasonyeza *tshintu*
5 kwa awo m' kundandalika, kuti, Dinali m' mzinda wa Yopa
kupempera: ndimo m' tshoona dinaona tshoona, tshiwira
tshimodzi kutsika, monga tshinali tshopfunda tshatshikuru
tshinatsitsidwa kwa kumwamba ndi dzipe dzinai; ndimo
6 tshinafika inde kwa ine: pa itsho ntawi dinayang'anitsa,
dinaganiza, ndimo dinaona nyama za mapazi anai za pansi
7 ndi zirombo ndi zokwawa ndi mbalame za mwamba. Ndimo
dinamva anso liu kunena ndi ine, Uka, Petros; ipa nudia.
8 Koma dinanena, Si tshointsho, Mwini: tshifuka palibe
kantu kanko kapena kosatsuka sikanaloa palibe ntawi m
9 nkamwa mwanga. Koma liu linaiang'ka ntawi yatshiwiri
kwa mwamba, Tshomwe Mulungu watsuka, usapanga
10 tshanko. Ndimo tshimene tshinatshitidwa katatu: ndimo
11 zonse zinakokedwa anso m'mwamba. Ndimo ona, tsopano lino
antu atatu naima patsogolo nyumba momwe tinali, anatumi-
12 dwa kwa Kesareya kwa ine. Ndimo Nzimu unauza ine ku
muka nao, kupanga kulibe kulekana. Ndimo abali amene
asanu ndi modzi inso anatsagana ndi ine; ndimo tinaloa m'
13 nyumba ya muntu: ndimo natiuza bwanje anaona njelo

kuima m' nyumba yatshi, ndi kuti, Tumiza kwa Yopa,
nutenga Simon, dzina lina la emwe liri Petros; emwe 14
adzalankula mau ndi iwe, mwa kuti udzapulumutsidwa, iwe
ndi nyumba yako yonse. Ndimo monga dinaamba ku 15
lankula, Nzimu Woyera unagwa pa awo, inde monga pa ife
pa kwiamba. Ndimo dinakumbukila mau a Mwini, bwanje 16
kuti nanena, Yohane nditu anabapatiza ndi madzi; koma
mudzabapatizidwa ndi Nzimu Woyera. Ndimo ngati Mulungu 17
anapatsa kwa awo tshaulere tshofana monga *napatsa* anso
kwa ife, ntawi tinamvana ndi Mwini Yesu Kristu, dinali ani,
kuti dikaima pa Mulungu? Ndimo ntawi anamva zintu 18
zimene, nakala otshete, napambanitsa Mulungu, kuti, Pomwe
kwa Mitundu unso Mulungu wapatsa kutembenuza ntima
kwa moyo.

Ndimo awo omwe anabalalitsidwa pa sautso yomwe 19
inauka kwa Stefano anaenda monga kutali monga Fenike,
ndi Kipro, ndi Antiyokwe, kulankula mau ndi palibe
modzi koma kwa Ayuda oka. Koma anali ena a 20
awo, antu a Kipro ndi Kirene, omwe, ntawi anafika kwa
Antiyokwe, nalankula ndi Agrike enso, kuuza Mwini Yesu.
Ndi dzanja la Mwini linali ndi awo: ndi ambiri omwe 21
anamvana natembenuka kwa Mwini. Ndimo mbiri ndi awo 22
inafika ku makutu a eklesia lomwe linali m' Yerusalem:
ndimo natumiza Barnaba monga kutali monga Antiyokwe:
emwe, ntawi anafika, ndimo anaona kufatsa kwa Mulungu, 23
anasekera; ndimo nalungamitsa awo onse, kuti ndi kuyere-
keza kwa ntima akagwirizana ndi Mwini: kuti anali muntu 24
wabwino, ndimo wodzaza ndi Nzimu Woyera ndimo ndi
mvanu: ndi antu ambiri anaong'khetsedwa kwa Mwini.
Ndimo naturuka ku Tarso ku funira Saulos: ndimo ntawi 25
anampeza, natenga ie ku Antiyokwe. Ndimo kunali, kuti 26
inde kwa tshaka tshonse anasong'kanitswa ndi eklesia,
napunzitsa antu ambiri; ndimo kuti akupunzira anatshedwa
Akristu kuamba m' Antiyokwe.

Ndimo m' masiku amene aprofeti anatsika kwa Yerusalem 27
kwa Antiyokwe. Ndimo nauka modzi wa awo atshedwa 28
Agabo, nasonyeza ndi Nzimu kuti kudzakala njala yeikuru
pa dziko lonse: yomwe inafika m' masiku a Klaudiyo.
Ndimo akupunzira, antu onse kwa mpamvu yatshi, nayere- 29
keza ku tumiza kutandizira kwa abali omwe nakala m'
Yudeya: komwe enso natshita, kukutumiza kwa akuru ndi 30
dzanja la Barnaba ndi Saulos.

12 Ndimo pa ntawi imene Herode fumu yotshuka natu-
2 rutsa manja atshi ku sautsa ena a eklesia. Ndimo
napa Yakobi njiratshi wa Yohane ndi mpeni wa nkondo.
3 Ndimo ntawi naona kuti tshinaseketsa Ayuda, napitirira
ku gwira Petros anso. Ndi *adya* anali masiku a nkate
4 wopanga tshabe. Ndimo ntawi anagwira ie, namwika m'
nyumba ya ndima, napereka ie ku mwanai anai a
ankhondo ku dikira ie; kuyerekeza pambuiu Mpasika ku
5 turutsa ie kwa antu. Ndimo Petros anasungidwa m'
nyumba ya ndima: koma kupempera kunapangidwa kolimba
6 ndi eklesia ku Mulungu kwa ie. Ndimo ntawi Herode
anafuna kumturutsa, usiku womwe Petros analikugona
pakati pa ankhondo awiri, womangidwa ndi maunyolo
awiri: ndi akudikira patsogolo pa tshitseko nasunga nyumba
7 ya ndima. Ndimo ona, njelo wa Mwini naima ndi ie,
ndimo kuunika kunawala m' tshipinda: ndimo namenya
Petros pa kundu, namukitsa, kuti, Uka nsanga. Ndimo
8 maunyolo atshi anagwa kwa manja atshi. Ndimo njelo
nanena nai', Mangitsa, numanga dzikwakwata dzako. Ndimo
natshita tshointsho. Ndimo anena nai', Ponya tshopfunda
9 tshako pa iwe, nunditsata. Ndimo naturuka, natsata;
ndimo sanadziwa kuti tshinali tshanteradi tshomwe tshinatshi-
10 tidwa ndi njelo, koma naganiza naona tshoona. Ndimo
ntawi anapita kudikira kwa tshimodzi ndi kwa tshiwiri, nafika
kwa tshipata tshatshitsulo tshomwe tshitsogoza ku mzinda;
tshomwe tshinatseguka tshoka kwa awo: ndimo naturuka,
napita mwa kwalala limodzi; ndimo tsopano lino njelo
11 natshoka kwa ie. Ndimo ntawi Petros natsitsimuka, nati,
Tsopano didziwa kwa nteradi, kuti Mwini watumiza njelo
watshi ndimo wapulumutsa ine kwa dzanja la Herode, ndi
12 kwa kuyang'anira konse kwa antu a Ayuda. Ndimo ntawi
anaganiza ndi *tshintu*, nafika ku nyumba ya Mariya amai
atshi a Yohane dzina lina la emwe linali Marko; pomwe
13 ambiri anasong'kanitswa ndimo analikupempera. Ndimo
ntawi nagogoda pa tshitseko tsha tshipata, butu linafika
14 ku yang'ka, litshedwa Roda. Ndimo ntawi linadziwa liu la
Petros, silinatsegula tshipata tshifuka tsha tshimwemwe,
koma linatamangira umo, ndimo linauza kuti Petros naima
15 patsogolo pa tshipata. Ndimo nanena ndi ilo, Uli wamisala.
Koma ilo linatshimika m' nteradi kuti tshinali tshointsho
16 nditu. Ndimo nati, Ali njelo watshi. Koma Petros ana-
gogodabe: ndimo ntawi anatsegula, namona, nazizwa.

Koma ie, kukodola kwa awo ndi dzanja ku tontola, nauza 17
awo bwanje Mwini naturutsa ie mwa nyumba ya ndima.
Ndimo nati, Uza zintu zimenezi kwa Yakobi, ndi kwa abali.
Ndimo natshoka, namuka ku malo ena. Ndimo monga 18
nsanga monga unali msana, kunali kuzingalidwa si kwaku-
ng'ono mwa ankhondo, Petros kunali bwanje. Ndimo 19
ntawi Herode anafunira ie, ndimo sanampeza, nafunsitsa
akudikira, nauza kuti akapedwa. Ndimo natsika kwa
Yudeya ku Kesareya, nakala apo.

Ndimo nakwia kwambirindi Akutire ndi Akutsidon: ndimo 20
nafika ndi ntima umodzi kwa ie, ndimo, anapanga Blasto
dindo wa fumu yotshuka mbali wao, napempa ntendere,
tshifuka dziko lao linaetedwa kwa dziko la fumu yotshuka.
Ndimo pa siku lokazika Herode nadzibvala m' nsaru 21
zotshuka, nakala pa mpando wotshuka, napanga kugwira-
moyo kwa awo. Ndimo antu napfula, *kuti*, Liu la mulungu, 22
ndimo si la muntu. Ndimo tsopano lino njelo wa Mwini 23
namenya ie, tshifuka sanapatsa kupambana kwa Mulungu:
ndimo anadibwa ndi zimbozi, nasirizika.

Koma mau a Mulungu nakula napindula. 24

Ndimo Barnaba ndi Saulos nabwera ku Yerusalem, ntawi 25
anadzaza kuimirira kwao, kutenga nao Yohane dzina lina
la emwe linali Marko.

Ndimo kunali pa Antiyokwe, m' eklesia lomwe linali *apo*, 13
aprofeti ndi apunzitsi, Barnaba, ndi Simon emwe natshedwa
Nigeri, ndi Lukiyo wa Kirene, ndi Manayen mpwatshi
wosunga wa Herode woweruza wa tshinai, ndi Saulos.
Ndimo monga naimirira kwa Mwini, naleka kudia, Nzimu 2
Woyera unanena, Sang'ka kwa ine Barnaba ndi Saulos kwa
ntshito kwa yomwe daitana awo. Pomwe, ntawi analeka 3
kudia napempera naika manja ao pa awo, natumiza awo.

Ndimo awo, kutumidwa ndi Nzimu Woyera, natsika ku 4
Selukiya; ndi kwa uko naenda ndi matanga ku Kipro.
Ndimo ntawi anali pa Salamis, nauza mau a Mulungu m' 5
masinagoge a Ayuda: ndimo anali inso ndi Yohane monga
woimirira wao. Ndimo ntawi anamuka mwa tshisi tshonse 6
kwa Pafo, napeza woombeza ula modzi, mprofeti wonama,
Myuda, dzina la emwe linali Barayesu; emwe anali ndi 7
mbiri, Sergo Paulos, muntu wa kudziwitsa. Amene
naitana kwa ie Barnaba ndi Saulos, nafuna ku mva mau a
Mulungu. Koma Elima woombeza ula (kuti tshointsho 8
liri dzina latshi ndi kusanduka) natsutsa awo, kufuna ku

9 balutsa mbiri kwa mvanu. Koma Saulos, emwe enso
*atshedwa* Paulos, wodzaza ndi Nzimu Woyera, nayang'anitsa
10 ie, nati, O wodzaza ndi tshinyengo tshonse ndi mpulupulu
zonse mwana iwe wa diabolos, liwongo iwe la kudeka konse,
kodi usafuna ku leka ku tembenuza njira zodeka za Mwini?
11 Ndimo tsopano, ona, dzanja la Mwini liri pa iwe, ndimo
udzakala ndi kungu, sikuona dzua kwa ntawi. Ndimo
tsopano lino zinagwa pa ie nkhungu ndi ndima; ndimo
naendaenda kufunira wina ku tsogolera ie ndi dzanja.
12 Ndimo mbiri, ntawi naona tshiani tshinatshitidwa, namvana,
kuzizwa kwa kupunzitsa kwa Mwini.
13 Ndimo Paulos ndi gulu latshi naenda ndi matanga kwa Pafo,
nafika ku Perga m' Pamfiliya: ndimo Yohane natshoka kwa
14 awo, nabwera ku Yerusalem. Koma awo, kupita kwa
Perga, nafika kwa Antiyokwe wa Pisidiya; ndimo naloa m'
15 sinagoge pa dzua la sabata, nakala pansi. Ndimo pambuiu
pa kuwerenga kwa mau ndi aprofeti akuru a sinagoge
natumiza kwa awo, kuti, Amuna, abali, ngati mupotshera
16 mau a kulungamitsa kwa antu, nenani. Ndimo Paulos
nauka, ndi kukodola ndi dzanja nati,
Amuna, Asirayeli, ndi inu nomwe muopa Mulungu, mumve.
17 Mulungu wa antu amene Sirayeli nasang'ka atatu atu,
napambanitsa antu ntawi nakala alendo m' dziko la Yiputa,
18 ndimo ndi nkono wolimba natsogoza awo mwa ilo. Ndimo
kwa pa ntawi ya dzaka makumi anai anamva makalidwe ao m'
19 tshipululu. Ndimo ntawi anamwaza mitundu isanu ndi iwiri
m' dziko la Kanane, napatsa *awo* dziko lao kwa tsholoa, kwa
20 dzaka mazana anai ndi makumi asanu: ndimo pambuiu zintu
zimenezi napatsa *awo* oweruza kwa ntawi ya Samuweli
21 mprofeti. Ndimo pambuiu nafunsa kwa fumu yotshuka:
ndimo Mulungu napatsa awo Saule mwana wa Kishe, muntu
wa fuko la Benyamin, kwa ntawi ya dzaka makumi anai.
22 Ndimo ntawi anatshotsa ie, naukitsa Davide kukala fumu
yotshuka yao; kwa emwe enso namariza, nati, Dapeza
Davide mwana wa Yishayi, muntu kwa ntima wanga, emwe
23 adzatshita kufuna kwanga konse. Wa mbeu ya muntu
amene Mulungu kwa kulonjezana watenga kwa Sirayeli
24 Mpulumutsi, Yesu; ntawi Yohane anauza poiamba patsogolo
pa kudza kwatshi mbapatisma la kutembenuza ntima ku
25 antu onse a Sirayeli. Ndimo monga Yohane analikudzaza
kupita kwatshi, nati, Muganiza kuti diri ani? Sindiri *ie*.
Koma ona, kudza modzi pambuiu pa ine, dzikwakwata dza

mapazi a emwe sindienera ku masula. Amuna, abali, ana a 26
fuko la Abraham, ndi amenewo mwa inu omwe aopa Mulungu,
kwa ife mau a kupulumutsa kumene atumidwa. Kuti awo 27
omwe akala m' Yerusalem, ndi oweruza ao, tshifuka sana-
mdziwa, kapena maliu a aprofeti omwe awerengedwa pa
masabata onse, nadzaza *awo* ndi kusutsa *ie*. Ndimo ngati 28
sanapeza tshifukwa tsha imfa *mwa ie*, kosuntira nafunsa
Pilato kuti anganapedwa. Ndimo ntawi anadzaza zintu 29
zonse zomwe zinalembedwa ndi ie, natsitsa ie kwa ntengo,
namwika m' mwanda. Koma Mulungu naukitsa ie kwa 30
akufa: ndimo anaonedwa kwa masiku ambiri ndi awo omwe 31
nakwera ndi ie kwa Galileya ku Yerusalem, omwe ali
tsopano omariza atshi kwa antu. Ndimo titenga kwa inu 32
makalidwe abwino a kulonjezana kunapangidwa kwa atate,
bwanje kuti Mulungu wadzaza kumene kwa ana atu, mwa 33
kuti naukitsa Yesu; monga anso alembedwa m' salmo
latshiwiri, Uli Mwana wanga, siku limene dabala iwe.
Ndimo monga ndi kuti naukitsa ie kwa akufa, tsopano 34
palibe enso ku bwera kwa kubvunda, wanena tshointsho,
Didzapatsa inu *madalo* oyera ndi olimbika a Davide.
Tshifuka anena anso m' *salmo* lina, Usadzapatsa Woyera 35
wako ku ona kubvunda. Kuti Davide, pambuiu m' fuko 36
latshi anaimirira kuweruza kwa Mulungu, nagona, naikidwa
kwa atatu atshi, naona kubvunda: koma ie emwe Mulungu 37
anaukitsa sanaona kubvunda. Ndimo kudziwidwa kwa inu, 38
amuna, abali, kuti mwa muntu amene kubweza kwa zoipa ku
uzidwa kwa inu: ndimo ndi ie onse omwe amvana adeke- 39
tsedwa kwa zintu zonse, kwa zomwe simudziwa ku deketsedwa
ndi mau a Moses. Ndimo tshenjerani, kani tshimene tshidza 40
pa *inu*, tshomwe tshinenedwa mwa aprofeti;

Onani, onyoza inu, ndi zizwitswani, ndi mwazani; 41
Kuti ditshita ntshito m' masiku anu,
Ntshito yomwe musadzamvana konse, ngati modzi
aiuza kwa inu.

Ndimo monga naturuka, napempa kuti mau amene 42
anangolankulidwa kwa awo sabata lina. Ndimo ntawi 43
sinagoge linabalalika, ambiri a Ayuda ndi a openduka
opembedza, natsata Paulos ndi Barnaba: omwe, kulankula
ndi awo, nafulumiza awo ku kalabe m' kufatsa kwa
Mulungu.

Ndimo sabata lina pafupi ndi mzinda wonse unasong'kani- 44
dwa ku mva mau a Mulungu. Koma ntawi Ayuda naona 45

antu ambiri, anadzazidwa ndi nsanje, nadzudzula zintu
46 zomwe zinalankulidwa ndi Paulos, natukwana. Ndimo
Paulos ndi Barnaba nanena kolimba, nati, Kukanakala kuti
mau a Mulungu akanalankulidwa poiamba kwa inu. Mwa
kuti muaturutsa kwa inu, ndimo muweruza inu noka
osaenera kwa moyo wosamariza, ona, titembenuka kwa
47 Mitundu. Kuti tshointsho Mwini wauza ife, *kuti*,

Daika iwe kwa kuunika kwa Mitundu,
Kuti ukakala kwa kupulumutsa kwa malo akutali a dziko.

48 Ndimo monga Mitundu inamva amene, nisekera, nipamba-
nitsa mau a Mulungu: ndimo monga yambiri monga ina-
49 loezedwa ku moyo wosamariza inamvana. Ndimo mau a
50 Mwini anayanikidwa mwa dziko lonse. Koma Ayuda
nafulumiza akazi opembedza a makalidwe olemerera, ndi
antu akuru a mzinda, nakantshizira kuzunza pa Paulos ndi
51 Barnaba, naturutsa awa ku miraga yao. Koma nasansa
52 fumbi la mapazi ao pa awo, nadza kwa Koniyon. Ndimo
akupunzira nadzazidwa ndi tshimwemwe ndimo ndi Nzimu
Woyera.

14 Ndimo kunali m' Koniyon, kuti naloa pa modzi mwa
sinagoge la Ayuda, nalankula tshointsho, kuti antu ambiri
2 a Ayuda ndi a Agrike namvana. Koma Ayuda omwe anali
osamvera nakantshizira mizimu ya Mitundu, napanga iyo ku
3 kala yakukwia pa abali. Ndimo ntawi yeitali nakala *apo*
kunena kolimbika m' Mwini, emwe namariza ndi mau a
kufatsa kwatshi, kupatsa zizindikilo ndi zozizwa kutshitidwa
4 ndi manja ao. Koma antu ambiri a mzinda anagawidwa;
ndi pande linakala ndi Ayuda, ndi pande ndi apostile.
5 Ndimo ntawi kuteta kunapangidwa kwa Mitundu ndi kwa
Ayuda ndi kwa oweruza ao, ku tshita koipa nawo, ndi
6 ku ponya miala pa awo, naamba ku dziwa ndi tshimene,
natawa ku mizinda ya Likawoniya, Lystra ndi Derbe, ndi
7 dziko lozungulira: ndimo apo nauza ivangeli.
8 Ndimo pa Lystra nakala muntu modzi, wopanda mpamvu
m' mapazi atshi, wopunduka miendo kwa tshibaliro tsha amai
9 atshi, emwe palibe ntawi anaenda. Emwe anamva Paulos
kulankula: emwe, kuyang'anitsa ie, ndi kuona kuti anali
10 ndi mvanu ku pulumutsidwa, nati ndi liu lalikuru, Ima ndi
11 mapazi ako. Ndimo nalumpa naendaenda. Ndimo ntawi
antu ambiri anaona tshomwe Paulos anatshita, natukula liu
lao, kuti m' liu la Likawoniya, Milungu inatsika kwa ife m

kufaniza kwa antu. Ndimo natshedwa Barnaba, Zeyos; ndi 12
Paulos, Hermes, tshifuka anali wonena wopambana. Ndimo 13
ndzukuru wa Zeyos, tempile la emwe linali patsogolo pa
mzinda, natenga zing'ombe ndi zingwe za malua kwa dzipata,
ndimo anafuna ku tsira nsembe ndi antu ambiri. Koma 14
ntawi apostile, Barnaba ndi Paulos, anamva, anang'amba
miinjiro yao, nalumpa patsogolo mwa antu ambiri, kupfula
ndi kuti, Mafumu, bwanje mutshita zintu zimenezi? Ife 15
enso tiri antu a makalidwe ofana ndi inu, ndimo titengera
inu makalidwe abwino, kuti mukatembenuka kwa zintu
zimenezi zautsiru kwa Mulungu wamoyo, emwe napanga
kumwamba ndi dziko ndi nyanja, ndi zonse zomwe ziri mwa
izo: emwe m' mafuko anapita anamva mitundu yonse ku 16
pita m' njira zao. Ndimo kosuntira sanaleka ie eka 17
wopanda kumariza, mwa kuti natshita ubwino, napatsa inu
kwa kumwamba mvula ndi nsiku zadzobala, kudzaza mitima
yanu ndi kudia ndi kusekera. Ndimo ndi mau amene na- 18
leketsa kopereweza antu ambiri kwa ku tsira nsembe kwa
awo.

Koma kunafika uko Ayuda kwa Antiyokwe ndi Koniyon: 19
ndimo anakantshizira antu ambiri, naponya miala pa Paulos,
namkoka ku mzinda, kuganizaganiza kuti anafa. Koma 20
monga akupunzira naima kozungulira ie, nauka, naloa
muzinda: ndimo pa mawa naturuka ndi Barnaba ku
Derbe. Ndimo ntawi anauza ivangeli ku mzinda umene, 21
ndimo anapanga akupunzira ambiri, nabwera ku Listra, ndi
ku Koniyon, ndi ku Antiyokwe, kulimbikitsa mizimu ya 22
akupunzira, kutaulira awo ku kalabe mwa mvanu, ndimo
kuti mwa masautso ambiri tikanaloa m' dziko la Mulungu.
Ndimo ntawi analoeza akuru kwa awo m' maeklesia onse, 23
ndi anapempera ndi kuleka kudia, nabvomereza awo kwa
Mwini, ndi emwe anamvana. Ndimo napita pakati pa 24
Pisidiya, nafika kwa Pamfiliya. Ndimo ntawi analankula 25
mau m' Perga, natsika ku Atiliya; ndimo uko naenda ndi
matanga ku Antiyokwe, kwa komwe anaperekedwa kwa 26
kufatsa kwa Mulungu kwa ntshito yomwe anadzaza. Ndimo 27
ntawi anafika, ndi anasong'kanitsa eklesia, anauza anso zintu
zonse zomwe Mulungu anazitshita nao, ndimo bwanje kuti
anatsegula tshitseko tsha mvanu kwa Mitundu. Ndimo 28
nakala si ntawi yeing'ono ndi akupunzira.

Ndimo antu ena natsika kwa Yudeya napunzitsa abali, 15
*kuti*, Kani mudulidwa pambuiu pa mwambi wa Moses,

2 musadziwa ku pulumutsidwa. Ndimo ntawi Paulos ndi
Barnaba napotshera kukanirana si kwakung'ono ndi kufunsa
nao, *abali* naloeza kuti Paulos ndi Barnaba, ndi ena a awo,
akakwera ku Yerusalem kwa apostile ndi akuru ndi funso
3 limene. Ndimo awo, kuperekezedwa pa njira yao ndi
eklesia, napita pakati pa Fenike ndi Samariya, kuuza kute-
mbenuza kwa Mitundu: ndimo nasekeretsa kwambiri abali
4 onse. Ndimo ntawi anafika ku Yerusalem, analandiridwa ndi
eklesia ndi apostile ndi akuru, ndimo nauza anso zintu zonse
5 zomwe Mulungu anatshita ndi awo. Koma anauka ena a
kugawa kwa Afarisi omwe namvana, kuti, Tshiri tsha-
bwino ku dula awo, ndi ku uza awo ku sunga mau a
Moses.

6 Ndimo apostile ndi akuru anasong'kanitswa ku ganiza ndi
7 tshintu tshimene. Ndimo ntawi kunali kufunsa kwambiri,
Petros nauka, nanena nao,

Amuna, abali, mudziwa bwanje kuti m' masiku akali Mu-
lungu nasang'ka mwa inu, kuti ndi nkamwa mwanga Mitundu
8 ikamva mau a ivangeli, ndi ikamvana. Ndimo Mulungu,
emwe adziwa ntima, namariza nayo, kupatsa iyo Nzimu
9 Woyera, inde monga natshita kwa ife; ndimo sanapanga
kulekana pakati pa ife ndi iyo, kutsuka mitima yao ndi
10 mvanu. Ndimo tsopano bwanje muyesa Mulungu, kuti
mukaika tshigologolo pa kosi la akupunzira, tshomwe kapena
si atatu atu, kapena ife sitinali ndi mpamvu ku nyamula?
11 Koma timvana kuti tidzapulumutsidwa mwa kufatsa kwa
Mwini Yesu, modzimodzi ndi iyo.

12 Ndimo antu ambiri onse natontola; namva Barnaba ndi
Paulos kunena anso zizindikilo ndi zozizwa zomwe Mulungu
13 anazitshita mwa Mitundu ndi awo. Ndimo pambuiu
anatontola, Yakobi naiang'ka, kuti,

14 Amuna, abali, imvani ine: Simeyon wauza anso bwanje
poiamba Mulungu anatshezera Mitundu, ku tshotsa mwa iyo
15 antu kwa dzina latshi. Ndimo kwa tshimene mau a aprofeti
agwirizana; monga alembedwa,

16 Pambuiu zintu zimenezi didzabwera,
Ndimo didzamanga anso msasa wa Davide, womwe unagwa;
Ndimo didzamanga anso mapasuko a iwo,
Ndimo didzauimitsa:
17 Kuti otsala a antu angofunira Mwini,
Ndi Mitundu yonse, pa yomwe dzina langa litshedwa,

Ati Mwini, emwe apanga zintu zimenezi zodziwidwa 18
kwa kuamba kwa dziko.
Mwa kuti kuweruza kwanga kuli, kuti sitibvuta awo omwe 19
kwa Mitundu atembenuka kwa Mulungu; koma kuti tilembe 20
kwa awo, kuti aleke kwa madetso a mafano, ndi kwa dama,
ndi kwa tshomwe tshikwipidwa, ndi kwa mwazi. Kuti 21
Moses kwa mafuko akali apotshera m' mizinda yonse awo
omwe auza ie, kuwerengedwa m' masinagoge masabata
onse.

Pomwe kuganizidwa bwino ku apostile ndi akuru, ndi 22
eklesia lonse, ku sang'ka antu mwa gulu lao, ndi ku tumiza
awo ku Antiyokwe, ndi Paulos ndi Barnaba; Yuda atshe-
dwa Barsaba, ndi Sila, antu akuru mwa abali: ndimo 23
nalemba *tshointshi* ndi awo, Apostile ndi abali akuru kwa
abali omwe ali a Mitundu mwa Antiyokwe ndi Siriya ndi
Kilikia, kuutsa: Mwa kuti tamva kuti ena omwe naturuka 24
kwa ife anabvuta inu ndi mau, kupasula mizimu yanu;
kwa omwe sitinapatsa mau; kuganizidwa bwino kwa ife, 25
kunafika ku ntima umodzi, ku sang'ka antu ndi ku tumiza
awo kwa inu ndi Barnaba ndi Paulos okondedwa atu, antu 26
omwe anadzitaia mioyo yao kwa dzina la Mwini watu Yesu
Kristu. Ndimo tatumiza Yuda ndi Sila, omwe awo oka 27
anso adzauza inu zintu zomwe ndi mau a nkamwa. Kuti 28
kunaganizidwa bwino kwa Nzimu Woyera, ndi kwa ife, ku
ika pa inu palibe katundu wang'kuru wopambana zintu
zimene zofunidwa; kuti muleka kwa zintu zotsiridwa kwa 29
mafano, ndi kwa mwazi, ndi kwa zintu zokwipidwa, ndi kwa
dama; kwa zomwe ngati musunga inu noka, tshidzakala
bwino ndi inu. Kalani bwino.

Ndimo awo, ntawi anatshotsedwa, natsika kwa Antiyo- 30
kwe; ndimo anasong'kanitsa antu ambiri, anapereka epistola.
Ndimo ntawi analiwerenga, nasekera kwa kusangalatsa. 31
Ndi Yuda ndi Sila, ali awo oka anso aprofeti, nataulira 32
abali ndi mau ambiri, nalimbikitsa awo. Ndimo pambuiu 33
anakala ntawi yeing'ono *apo*, anatshotsedwa m' ntendere
kwa abali kwa awo omwe anaturutsa awo. Koma Paulos 35
ndi Barnaba nakala m' Antiyokwe, kupunzitsa ndi kuuza
mau a Mwini, ndi ambiri ena anso.

Ndimo pambuiu masiku ena Paulos nanena ndi Barnaba, 36
Tibwere tsopano ndimo titsheze ndi abali m' mizinda yonse
mwa iyo tinauza mau a Mwini, *ndimo tione* bwanje akala.
Ndimo Barnaba nafuna ku tenga nao Yohane enso, emwe 37

38 natshedwa Marko. Koma Paulos wosaganiza bwino ku
tenga nao iemwe napambuka kwa awo kwa Pamfiliya, ndimo
39 sanapita nao kwa ntshito. Ndimo kunauka kukangana
kolimba, tshointshi kuti nalekana, ndi Barnaba natenga
40 Marko ndi ie, naenda ndi matanga kwa Kipro; koma
Paulos nasang'ka Sila, naturuka, kunabvomerezedwa ndi
41 abali kwa kufatsa kwa Mwini. Ndimo napita pakati pa
Siriya ndi Kilikiya, kulimbitsa maeklesia.
16 Ndimo nadza anso ku Derbe ndi ku Listra: ndimo ona,
wakupunzira modzi anali apo, atshedwa Timote, mwana wa
Myuda wankazi emwe namvana; koma atatu atshi anali
2 Mgrike. Emwe anauzidwa bwino ndi abali omwe anali pa
3 Listra ndi Koniyon. Ie Paulos nafuna ku muka nai';
ndimo namtenga namdula tshifuka tsha Ayuda omwe anali m'
maiko amene: kuti nadziwa onse kuti atatu atshi anali
4 Mgrike. Ndimo monga napita pakati pa mizinda, napereka
awo mau ku sunga, omwe anaikidwa ndi apostile ndi akuru
5 omwe anali pa Yerusalem. Tshointsho maeklesia analimbi-
tsidwa m' mvanu, napindulidwa m' kuwerenga masiku onse.
6 Ndimo napita pakati pa dziko la Frigiya ndi Galatiya,
kunaletsedwa ndi Nzimu Woyera ku lankula mau m' Asiya;
7 ndimo ntawi anafika pandunji pa Misiya, nayesa ku loa m'
8 Bitiniya; ndimo Nzimu wa Yesu sunaleka awo; ndimo
9 kupita mbali mwa Misiya, natsika ku Trowa. Ndimo
tshoona tshinasonyeza ku Paulos usiku; Kunali muntu wa
Makedoniya kuima, kupempa ie, ndi kuti, Yambuka m'
10 Makedoniya, nutangata ife. Ndimo ntawi anaona tshoona,
tsopano lino tinafuna ku turuka m' Makedoniya, kumariza
kuti Mulungu anaitana ife ku uza ivangeli kwa awo.
11 Ndimo kuenda ndi matanga kwa Trowa, tipanga kupita
kolungama ku Samotrake, ndimo siku lotsata ku Neyapo-
12 lis; ndi kwa uko kwa Filipi, womwe uli mzinda wa Make-
doniya, woiamba wa dziko, koloni *la Aroma:* ndimo tinali
13 m' mzinda umene kukala masiku ena. Ndimo pa dzua la
sabata tinaturuka kunja kwa tshipata mbali mwa ntsinje,
pomwe tinaganizaganiza analipo malo a kupempera; ndimo
tinakala pansi, nalankula ndi akazi omwe anasong'kana.
14 Ndimo nkazi wina atshedwa Lidiya, wogulitsa wa tshaku-
detsa, wa mzinda wa Tiyatira, modzi emwe napembedza
Mulungu, anamva ife: ntima wa emwe Mwini anatsegula,
kusamala ndi zintu zomwe zinalankulidwa ndi Paulos.
15 Ndimo ntawi anabapatizidwa, ndi banja latshi, napempa ife,

kuti, Ngatı mwaweruza ine ku kala ndi mvanu kwa Mwini,
loani m' nyumba yanga, ndimo kalani *umo*. Ndimo nafulu-
miza ife.

Ndimo kunali, monga tinalikupita ku malo a kupempera, 16
kuti butu limodzi liri ndi nzimu wa ulaula linakomana ndi ife,
lomwe linatenga ambuiye atshi kupindula kwambiri ndi
kuombeza ula. Lomwe kutsata Paulos ndi ife linapfula, 17
kuti, Antu amene ali akapolo a Mulungu Wang'kuru
Wopambana, omwe auza kwa inu njira ya kupulumutsa.
Ndimo tshimene linatshita kwa masiku ambiri. Koma 18
Paulos, kunantentemeredwa kwambiri, natembenuka nanena
ndi nzimu, Diuza iwe m' dzina la Yesu Kristu ku turuka
mwa ilo. Ndimo unaturuka mwa ora limene.

Koma ntawi ambuiye atshi naona kuti kulingalira kwa 19
kupindula kwao kunatshoka, nagwira Paulos ndi Sila,
nakoka awo m' malo a maronda patsogolo pa oweruza,
ndimo ntawi anatenga awo kwa akazembe, nati, Antu 20
amene, ali Ayuda, antentemeretsa kwambiri mzinda watu,
nauza makalidwe omwe osali amau kwa ife ku landira, 21
kapena ku sunga, tiri Aroma. Ndimo antu ambiri nauka 22
pa modzi pa awo: ndi akazembe nang'amba miinjiro yao
kwa awo, nauza ku menya awo ndi zintole. Ndimo ntawi 23
namenya mikakato yambiri pa awo, naaponya m' nyumba
ya ndima, kuuza ndindo wa nyumba ya ndima ku sunga
awo kolimbika: emwe, kunalandira kuuza kotere, naponya 24
awo m' tshipinda tsha nyumba ya ndima tshapakati,
namanga mapazi ao kolimba m' magoli. Koma kwa pakati 25
pa usiku Paulos ndi Sila analikupempera ndi kuimba
zinyimbo kwa Mulungu, ndi omangidwa analikumva awo;
Ndimo nsangansanga kunali tshibvomezi tshatshikuru, 26
monga kuti maziko a nyumba ya ndima anagwedezedwa:
ndimo tsopano lino dzitseko dzonse dzinatsegulidwa; ndi
zomanga za onse zinamasulidwa. Ndimo ndindo wa 27
nyumba ya ndima anadzukitswa kwa tulo, ndimo kuona
dzitseko dza nyumba ya ndima dzotsegudwa, naturutsa
mpeni watshi wa nkondo, ndimo natofuna kudzipa, kuga-
nizaganiza kuti omangidwa anapulumuka. Koma Paulos 28
napfula ndi liu lalikuru, kuti, Usadzipweteka: kuti tiri tonse
muno. Ndimo naitana kwa miuni, nalumpira umo, ndimo, 29
kuntuntumira ndi kuopa, nagwa patsogolo pa Paulos ndi
Sila, naaturutsa, nati, Mafumu, kodi dikanatshita tshiani ku 30
pulumutsidwa? Ndimo nati, Mvana ndi Mwini Yesu, ndimo 31

32 udzapulumutsidwa, iwe ndi nyumba yako. Ndimo nala-
nkula mau a Mwini ndi ie, ndi onse omwe anali m' nyumba
33 yatshi. Ndimo natenga awo ora lomwe la usiku, natsuka
mikakato yao; nababapatizidwa, ie ndi onse atshi, tsopano lino.
34 Ndimo nakweretsa awo m' nyumba yatshi, naika kudia
patsogolo pa awo, nasekera kwambiri, ndi nyumba yatshi
yonse, anamvana ndi Mulungu.
35 Koma ntawi linali siku, akazembe natumiza anyamata ao,
36 kuti, Masula antu amene. Ndimo ndindo wa nyumba ya
ndima nauza mau kwa Paulos, *kuti*, Akazembe anatumiza
ku masula inu; ndimo tsopano turukani, mukani m'
37 ntendere. Koma Paulos nanena nao, Anamenya ife poyera,
osasutsidwa, antu omwe ali Aroma, naponya ife m' nyumba
ya ndima; ndimo tsopano kodi aturutsa ife kutseri? iai
38 nditu; koma afike awo oka ndimo atiturutsa. Ndimo
anyamata nauza mau amene kwa akazembe: ndimo naopa,
39 ntawi anamva kuti anali Aroma; ndimo nadza napempa
awo; ndimo ntawi anaturutsa awo, nafunsa awo ku tshoka
40 kwa mzinda. Ndimo naturuka nyumba ya ndima, naloa m'
*nyumba ya* Lidiya: ndimo ntawi anaona abali, nasangalatsa
awo, namuka.

17 Ndimo ntawi anapita pakati pa Amfipolis ndi Apoloniya,
nafika ku Tesalonika, pomwe linali sinagoge la Ayuda:
2 ndimo Paulos, monga makalidwe atshi anali, naloa kwa awo,
ndimo kwa masiku a sabata atatu nasing'kasing'ka ndi
3 awo kwa malemba, kutsegula ndi kutero, kuti Kristu
akanamva, ndi ku uka anso kwa akufa; ndi kuti Yesu
4 amene, emwe, *nati*, diuza kwa inu, ali Kristu. Ndi ena a
awo anakantshirizidwa, napatikana ndi Paulos ndi Sila; ndi
a Agrike opembedza antu ambiri, ndi a akazi akuru si
5 owereng'jeka. Koma Ayuda, kusuntidwa ndi nsanje, na-
tenga ku awo antu ena oipa a apokoso, ndimo kusong'ka-
nitsa antu ambiri, napanga mzinda pokoso; ndi kulowerera
nyumba ya Yason, nafuna ku turutsa awo kwa antu.
6 Ndimo ntawi sanapeza awo, nakoka Yason ndi abali ena
patsogolo pa oweruza a mzinda, kupfula, amene omwe
7 anatembenuza dziko ali kuno onso; omwe Yason walandira:
ndi amene onse atshita pa mau a Kesare, kunena kuti
8 iri fumu yotshuka ina, *modzi* Yesu. Ndimo anantente-
mera antu ambiri ndi oweruza a mzinda, ntawi anamva
9 zintu zimenezi. Ndimo ntawi anatenga tshigwiriro kwa
Yason ndi otsala, namasula awo.

Ndimo abali tsopano lino natshotsa Paulos ndi Sila usiku 10
kwa Bereya: omwe ntawi anafika uko naloa m' sinagoge la
Ayuda. Ndimo amenewa anali otshuka opambana amenewo 11
m' Tesalonika, mwa kuti analandira mau ndi kuta konse kwa
muwongo, kuyang'anira malemba masiku onse, ngati zintu
zimenezi zinali tshointsho. Ndimo ambiri a awo namvana; 12
anso a akazi Agrike a makalidwe otshuka, ndi a antu, si
owereng'jeka. Koma ntawi Ayuda a Tesalonika anali ndi 13
kudziwa kuti mau a Mulungu anauzidwa ndi Paulos pa
Bereya anso, nafika uko onso, kufulumiza ndi kuntentemera
antu ambiri. Ndimo pomwe tsopano lino abali natshotsa 14
Paulos ku enda monga kutali monga ku nyanja: ndimo Sila
ndi Timote anakalabe apo. Koma awo omwe naperekeza 15
Paulos namtenga monga kutali monga Atene: ndimo kula-
ndira mau kwa Sila ndi Timote kuti akafika kwa ie ndi
nsangu wonse, namuka.

Ndimo ntawi Paulos nalindira awo pa Atene, nzimu 16
watshi unaukitswa mwa ie, monga naona mzinda wodzaza
ndi mafano. Ndimo nasing'kasing'ka m' sinagoge ndi 17
Ayuda ndi antu opembedza, ndi m' malo a maronda masiku
onse ndi awo omwe nakomana nai'. Ndi ena anso a okonda- 18
nzeru a Aepikure ndi Astoike nakomana nai'. Ndi ena
nati, Wolankuladadala amene afuna ku nena tshiani? ena,
Aonedwa ku li wakuuza wa ademon osadziwika: tshifuka
nauza Yesu ndi kuukirira. Ndimo nagwira ie, natenga ie 19
kwa Areyopago, kuti, Kodi tidziwe tshiani kupunzitsa kwa-
tsopano kumene kuli, komwe kulankulidwa ndi iwe? Kuti 20
utenga zintu zosazizwika zina kwa makutu atu: ndimo tifuna
ku dziwa tshiani zintu zimenezi zitantauza. (Ndimo 21
Akuatene onse ndi aulendo kukala apo napisa ntawi zao m'
palibe kantu kwina, koma kapena ku uza kapena ku mva
kantu katsopano kena.) Ndimo Paulos naima pakati pa 22
Areyopago, nati,

Amuna, Akuatene, m' zintu zonse diona kuti muli
opembedza opambana. Kuti monga dinapita, ndinayang'anira 23
zopembezedwa zanu, dinapeza anso katshisi ndi lemba
limene, Kwa Mulungu Wosadziwidwa. Ndimo tshomwe
kusadziwa mupembedza, tshimene diika patsogolo pa inu.
Mulungu emwe anapanga dziko ndi zintu zonse mwa ilo, ie, 24
ali Mwini wa mwamba ndi pansi, wosakala m' malo oyera
apangidwa ndi manja; kapena wosaimiririridwa ndi manja a 25
antu, monga ngati afunira kantu, kuona kuti ie eka apatsa

26 ku onse moyo, ndi pwea, ndi zintu zonse; ndimo napanga
kwa modzi, mitundu yonse ya antu ku kala pa nkope
yonse ya dziko, kunasonyeza nsiku *zao* zoikidwa, ndi
27 maliri a malo ao; kuti ikafuna Mulungu, ngati kapena
inangofufunyira ie, ndi ku peza ie, koma wosali kutali kwa
28 ife tonse: kuti mwa ie tikala ndi moyo, ndi tisunta, ndi tiri;
monga inde ena a opanga nyimbo anu ananena, Kuti tiri
29 inso ana atshi. Ndimo tiri ana a Mulungu, sitikanaganiza
kuti Umulungu uli wofana ndi golide, kapena silivere,
kapena mwala, zilembedwa ndi nzeru ndi ntintu za muntu.
30 Ndimo ntawi za kusadziwa Mulungu sanasamala; koma
tsopano auza antu kuti onse m' malo onse akatembenuza
31 ntima: mwa kuti monga waika siku, mwa lomwe adzawe-
ruza dziko m' kudeka ndi muntu emwe waloeza; ndi emwe
wapatsa kulimbikitsa kwa antu onse, mwa kuti waukitsa ie
kwa akufa.
32 Ndimo ntawi anamva ndi kuukirira kwa akufa, ena
natonza; koma ena nati, Tidzamva iwe ndi tshimene
33 ntawi ina anso. Tshointsho Paulos naturuka kwa awo.
34 Koma ena nakala ndi ie, namvana: mwa omwe enso anali
Diyonisiyo 'Mareyopago, ndi nkazi atshedwa Damaris,
ndi ena nao.
18 Pambuiu zintu zimenezi natshoka kwa Atene, nafika kwa
2 Korinte. Ndimo napeza Myuda modzi atshedwa Akwila,
muntu wa Ponto ndi fuko, kali pang'ono nafika kwa Yita-
liya, ndi nkazi watshi Prisila, tshifuka Klaudiyo anauza
Ayuda onse ku tshoka kwa Roma: ndimo ie nadza kwa
3 awo; ndimo tshifuka anali wa luso limodzi, nakala nao,
ndimo natshita; kuti ndi luso lao anali opanga misasa.
4 Ndimo nasing'ka m' sinagoge pa masabata onse, nakantshi-
zira Ayuda ndi Agrike.
5 Koma ntawi Sila ndi Timote natsika kwa Makedoniya,
Paulos nafulumizidwa ndi mau, kumariza kwa Ayuda kuti
6 Yesu anali Kristu. Ndimo ntawi nadzikaniza, natukwana,
nakutumula mwinjiro watshi, nanena nao, Mwazi wanu
*ukale* pa mitu yanu; diri wotsuka: kwa ntawi imene
7 didzapita ku Mitundu. Ndimo natshoka uko, naloa m'
nyumba ya muntu modzi atshedwa Tito Yusto, modzi emwe
napembedza Mulungu, nyumba ya emwe inali pafupi ndi
8 sinagoge. Ndimo Krispo, mkuru wa sinagoge, namvana
ndi Mwini ndi nyumba yatshi yonse; ndi ambiri a Akorinte
9 kumva, namvana, nabapatizidwa. Ndimo Mwini nanena

ndi Paulos usiku ndi tshoona, Usaopa, koma lankula, nusa-
tontola: kuti diri ndi iwe, ndimo palibe muntu adzalowerera 10
pa iwe ku pwetekesa iwe: kuti diri ndi antu ambiri
muzinda umene. Ndimo nakala *apo* tshaka tshimodzi ndi 11
miezi isanu ndi umodzi, kupunzitsa mau a Mulungu mwa awo.

Koma ntawi Galiyon anali mbiri wa Akaya, Ayuda ndi 12
ntima umodzi nauka pa Paulos, natenga ie patsogolo pa
mpando woyeruza, kuti, Muntu amene akantshizira antu ku 13
pembedza Mulungu pa mau. Koma ntawi Paulos natofuna 14
ku tsegula nkamwa mwatshi, Galiyon nanena ndi Ayuda,
Ngati nditu tshinali tshintu tsha tshimo kapena tsha urombo
woipa, O Ayuda inu, dingalira ifuna kuti dikamva ndi inu:
koma ngati ali mafunso ndi mau ndi maina ndi mau anu, 15
yang'anirani inu noka; sindifuna ku kala wowеruza wa
zintu zimenezi. Ndimo natshotsa awo kwa mpando wowe- 16
ruza. Ndimo onse nagwira Sostene, mkuru wa sinagoge, 17
nammenya patsogolo pa mpando woweruza. Ndimo Galiyon
sanasamala kwa kantu kwa zintu zimenezi.

Ndimo Paulos, anakala pambuiu pa tshimene inde masiku 18
ambiri, natsazika abali, naenda ndi matanga uko kwa
Siriya, ndimo ndi ie Prisila ndi Akwila; anameta mutu
watshi m' Kenkerea: kuti anali ndi kulumbira. Ndimo 19
nafika ku Feso, ndimo nasia awo apo: koma ie eka naloa
m' sinagoge, nasing'kasing'ka ndi Ayuda. Ndimo ntawi 20
nafunsa ie ku kala ntawi yeitali yopambana, sanalola; koma 21
kutsazika awo, ndi kuti, Didzabwera anso kwa inu, ngati
Mulungu afuna, namuka ndi matanga kwa Feso. Ndimo 22
ntawi nagwira ntunda kwa Kesareya, nakwera nautsa
eklesia, natsika kwa Antiyokwe. Ndimo anapisa ntawi ina 23
*apo*, natshoka, napita pakati pa dziko la Galatiya ndi Frigiya
kondandalika, kulimbikitsa akupunzira onse.

Ndimo Myuda modzi atshedwa Apolo, 'Malesandriya ndi 24
fuko, muntu wopunzitsa, nafika ku Feso; ndimo anali
wolimba m' malemba. Muntu amene anapunzitsidwa m' 25
njira ya Mwini; ndimo ali wotenta muzimu, nalankula,
napunzitsa koyang'anira zintu za Yesu, kudziwa koka
mbapatisma la Yohane: ndimo naamba ku nena kolimba 26
m' sinagoge. Koma ntawi Prisila ndi Akwila anamva ie,
namtenga kwa awo, napunzitsa kwa ie njira ya Mulungu
koyang'anira kopambana. Ndimo ntawi nafuna ku ya- 27
mbuka mwa Akaya, abali nakakamiza ie, nalemba kwa
akupunzira ku landira ie: ndimo ntawi anafika, natangata

28 kwambiri awo omwe anamvana mwa kufatsa: kuti nasing'-
ka kolimba Ayuda, *ndi kumene* poyera, kusonya ndi malemba
kuti Yesu anali Kristu.
19 Ndimo kunali, kuti, ntawi Apolo anali pa Korinte, Paulos
kunapita pakati pa dziko lantunda nafika kwa Feso, napeza
2 akupunzira ena: ndimo nanena nao, Kodi munalandira
Nzimu Woyera ntawi munamvana? Ndimo na*nena* nai',
Iai, sitinamva monga ambiri monga ngati Nzimu Woyera
3 una*patsidwa*. Nati, Ndimo mwa tshiani munabapatizidwa?
4 Ndimo nanena, Mwa mbapatisma la Yohane. Ndimo
Paulos nati, Yohane nabapatiza ndi mbapatisma la kute-
mbenuza ntima, kunena ndi antu, kuti akamvana pa ie
5 emwe akafika pambuiu pa ie, amene ali, pa Yesu. Ndimo
ntawi anamva tshimene, anabapatizidwa m' dzina la Mwini
6 Yesu. Ndimo ntawi Paulos anaika manja atshi pa awo,
Nzimu Woyera unafika pa awo; ndimo nalankula ndi
7 malilume, nalosa. Ndimo anali onse kwa antu kumi ndi
awiri.
8 Ndimo naloa m' sinagoge, nanena kolimba kwa ntawi ya
miezi itatu, kusing'ka ndi kukantshizira *monga ndi* zintu
9 za dziko la Mulungu. Koma ntawi ena analimbitsidwa ndi
osamvera, kulankula zoipa ndi Njira patsogolo pa antu
ambiri, natshoka kwa awo, nagawa akupunzira, kusing'ka
10 masiku onse m' skulu la Tirano. Ndimo tshimene tshina-
kalabe kwa ntawi ya dzaka dziwiri; monga kuti onse omwe
nakala m' Asiya anamva mau a Mwini, Ayuda ndi Agrike.
11 Ndimo Mulungu natshita mpamvu zosang'ka ndi manja a
12 Paulos: tshointshi kuti pa odwala zinatengedwa kwa tupi
latshi marenzo kapena maeprone, ndimo ntenda zinatshoka
13 kwa awo, ndi mizimu yoipa inaturuka. Koma ena anso a
Ayuda oendaenda, oturutsa, anatsanza kwa awo ku tshula pa
awo omwe anali ndi mizimu yoipa dzina la Mwini Yesu, kuti,
14 Dilimbika inu ndi Yesu emwe Paulos auza. Ndimo anali
ana amuna asanu ndi awiri a modzi Skeva, Myuda, ndzu-
15 kuru wang'kuru, omwe natshita tshimene. Ndimo nzimu
woipa unaiang'ka ndi unanena nao, Yesu didziwa, ndi
16 Paulo's didziwa; koma muli ani? Ndimo muntu mwa emwe
nzimu woipa unali nalumpa pa awo, napambana onse awiri
awo, napambanitsa pa awo, tshointshi kuti natawa m' nyumba
17 imene amariseke ndi olasidwa. Ndimo tshimene tshinadzi-
widwa kwa onse, Ayuda ndi Agrike, omwe nakala pa Feso;
ndi kuopa kunagwa pa awo onse, ndi dzina la Mwini Yesu

linakulitsidwa. Ambiri inso a omwe anamvana nadza, 18
kubvomera, ndi kuuza ntshito zao. Ndi si owereng'jeka a 19
awo omwe anatshita matsenga nasong'kanitsa mabuku ao,
naotsha awo m' kuona kwa onse: ndimo nawerenga ntengo
wa awo, naupeza zipinjiri za silivere mazousan makumi asanu.
Tshointsho mau a Mwini nakula kolimba, napambana. 20

Ndimo pambuiu zintu zimenezi zinata, Paulos nayerekeza 21
m' nzimu, ntawi anapita pakati pa Makedoniya ndi Akaya,
ku muka ku Yerusalem, kuti, Pambuiu dinali apo, dika-
naona anso Roma. Ndimo anatumiza m' Makedoniya awiri 22
a omwe naimirira kwa ie, Timote ndi Erasto, ie eka nakala
m' Asiya kwa ntawi.

Ndimo pa ntawi imene kunauka kutembenukatembenuka 23
si kwakung'ono ndi Njira. Kuti muntu modzi atshedwa 24
Demetriyo, wosula silivere, emwe napanga malo oyera a
silivere a Artemis, sanatenga ntshito yeing'ono kwa aluso;
omwe anasong'kanitsa, ndi otshita a luso lofana, nati, 25
Mafumu, mudziwa kuti ndi ntshito imene tiri ndi zolemera
zatu. Ndimo muona ndi ku mva, kuti si pa Feso woka, 26
koma pafupi ndi mwa Asiya lonse, Paulos amene waka-
ntshizira natembenuza antu ambiri, kuti yomwe yosali
milungu, yomwe ipangidwa ndi manja: ndimo si koka 27
kulipo kutsekerezwa kuti limene luso latu lifika mwa kupya-
pyaza; koma anso kuti tempile la mulungu-wankazi wang'-
kuru Artemis kupangidwa tshabe, ndimo kuti inde ie
akanatsitsidwa kwa kulemerera kwatshi, womwe Asiya lonse
ndi dziko zipembedza. Ndimo ntawi anamva tshimene, 28
anadzazidwa ndi kukwiira, napfula, kuti, Wang'kuru *ali*
Artemis wa Afeso. Ndi mzinda unadzazidwa ndi pokoso: 29
ndimo natamanga nsanga ndi ntima umodzi m' bwalo,
anagwira Gayo ndi Aristarko, antu a Makedoniya, olendo
anzatshi a Paulos. Ndimo ntawi Paulos nafuna ku loa kwa 30
antu, akupunzira sanaleka ie. Ndimo ena anso a oweruza a 31
Asiya, ali abali atshi, natumiza kwa ie, napempa ie si ku
dzitaia m' bwalo. Ndimo ena napfula tshintu tshimodzi, 32
ndi ena tshintu tshina: kuti kusong'kana kunali m' pokoso;
ndimo unyinji wa antu sunadziwa ndi tshiani unasong'-
kanira. Ndimo natenga Alesandire mwa antu ambiri, 33
Ayuda kuika ie patsogolo. Ndimo Alesandire nakodola ndi
dzanja, ndimo nakafuna ku panga kukana kwa antu. Koma 34
ntawi nadziwitsa kuti anali Myuda, onse ndi liu limodzi kwa
ntawi ya maora awiri napfula, Wang'kuru *ali* Artemis wa

35 Afeso. Ndimo ntawi wolembera-mzinda anatontoletsa antu
ambiri, anena, Amuna, Afeso, alipo muntu ndani emwe
wosadziwa bwanje kuti mzinda wa Afeso uli wosungira-
tempile wa Artemis wang'kuru, ndi wa *fano* lomwe linagwa
36 kwa Zeyos? Ndimo kuona kuti zintu zimenezi zosadziwa
ku kanidwa, mukanatontola, ndi ku tshita palibe kantu
37 katuku. Kuti mwatenga *kuno* antu amene, omwe osali
olanda a matempile kapena akutukwana a mulungu-
38 wankazi watu. Ndimo ngati Demetriyo, ndi aluso omwe
ali nai', ali ndi kantu pa muntu modzi, mphala ziri zotsegula,
39 ndimo alipo ambiri: lekani awo ku tshulana. Koma ngati
mufuna kantu kena ndi zintu zina, kadzaletsetsa m' kugwiri-
40 zana kondandalika. Kuti nditu tiri m' kutsekerezwa ku
tshulidwa ndi pokoso la siku limene, kunali kopanda tshifu-
kwa: ndimo monga ndi ilo sitidzadziwa ku wereng'jera ndi
41 kusong'kana kumene. Ndimo ntawi ananena tshointsho,
anabalalitsa kusong'kana.

20 Ndimo pambuiu pokoso linaleka, Paulos anatumiza kwa
akupunzira nataulira awo, natsazikana awo, natshoka ku
2 muka m' Makedoniya. Ndimo ntawi anapita mwa miraga
imene, ndimo anataulira awo kwambiri, nafika m' Grike.
3 Ndimo ntawi anakala *apo* miezi itatu, ndi kunje linaikidwa
pa ie ndi Ayuda, monga natofuna ku enda ndi matanga ku
4 Siriya, nayerekeza ku bwera pakati pa Makedoniya. Ndimo
anatsagana nai' monga kutali monga Asiya Sopatro wa
Bereya, *mwana* wa Piro; ndi a Atesalonika, Aristarko ndi
Sekundo; ndi Gayo wa Derbe, ndi Timote; ndi a Asiya,
5 Tikiko ndi Trofimo. Koma amene anapita patsogolo,
6 nalindira ife pa Trowa. Ndimo tinaenda ndi matanga kwa
Filipi pambuiu pa masiku a nkate wopanga tshabe, nafika
kwa awo ku Trowa m' masiku asanu; pomwe tinakala
masiku asanu ndi awiri.

7 Ndimo pa siku loamba la wiki, ntawi tinasong'kana ku
swa nkate, Paulos nalankula nao, kukantshizira ku tshoka
pa mawa; natanimpitsa kunena kwatshi kwa pakati pa
8 usiku. Ndimo inali miuni yambiri m' tshipinda tshaku-
9 mwamba, pomwe tinasong'kana. Ndimo nakala m' zanera
nyamata modzi atshedwa Yutiko, waguntumidwa ndi tulo;
ndimo monga Paulos nalankula kotanimpitsa kopambana,
kuguntumidwa ndi tulo tatshi nagwa kwa pamwamba tshi-
10 tatu, natukulidwa wakufa. Ndimo Paulos natsika, nagwa
pa ie, ndi kufumbatira ie nati, Musalongolola; kuti moyo

watshi uli mwa ie. Ndimo ntawi anakwera, ndimo anaswa 11
nkate, nadia, nalankula nao ntawi yambiri, inde kwa banda
kutsha, tshointsho namuka. Ndimo natenga nyamata wa- 12
moyo, ndimo anasangalatsidwa si kang'ono.

Koma ife, kunapita patsogolo ku tshombo, tinaenda ndi 13
matanga kwa Aso, apo kuyerekeza ku loetsa Paulos: kuti
tshointshi anasonyeza, kudzikantshizira ku muka pantunda.
Ndimo ntawi nakomana ndi ife pa Aso, tinaloetsa ie, nafika 14
ku Mitilene. Ndimo kuenda ndi matanga kwa uko, tinafika 15
siku lotsata pandunji pa Kiyo; ndimo dzua lina tinakotsheza
pa Samo; ndi siku lina tinafika kwa Mileto. Kuti Paulos 16
anakantshizira ku pitirira Feso, kuti sanangopisa ntawi
mwa Asiya; kuti analikufulumira, ngati anadziwa ku ta, ku
kala pa Yerusalem siku la Pentekoste.

Ndimo kwa Mileto natumiza kwa Feso, naitana kwa ie 17
akuru a eklesia. Ndimo ntawi anafika kwa ie, nanena nao, 18

Mudziwa inu noka, kwa siku loamba lomwe dinaturuka
pa Asiya, ndi makalidwe anje dinali ndi inu ntawi yonse,
kuimirira Mwini ndi kusadzitama konse kwa muwongo, 19
ndimo ndi misozi, ndimo ndi masautso omwe nafika pa ine
ndi makunje a Ayuda: bwanje kuti sindinaopa kwa ku uza 20
kwa inu kantu komwe kanapindulidwa, ndi kupunzitsa inu
poyera, ndi ku nyumba ndi nyumba, kumariza kwa Ayuda ndi 21
kwa Agrike kutembenuza ntima ku Mulungu, ndi mvanu kwa
Mwini watu Yesu Kristu. Ndimo tsopano, ona, dienda wo- 22
mangidwa m' nzimu kwa Yerusalem, sikudziwa zintu zomwe
zidzafika pa ine apo: kani kuti Nzimu Woyera umariza ndi 23
ine m' mizinda yonse, kunena kuti dzomangira ndi masautso
zilindira ine. Koma sindiganiza moyo wanga kwa kantu, 24
monga wokondedwa ndi ine ndeka, tshointsho kuti dingota
ulendo wanga, ndi kuimirira komwe dinalandira kwa Mwini
Yesu, ku mariza ndi ivangeli wa kufatsa kwa Mulungu.
Ndimo tsopano, ona, didziwa kuti inu nonse, mwa omwe 25
dinaenda ku uza dziko, adzaona nkope yanga palibe ntawi
ina. Mwa kuti dimariza ndi inu siku limene, kuti diri 26
woyera kwa mwazi wa antu onse. Kuti sindinaopa kwa ku- 27
uza kwa inu kuweruza konse kwa Mulungu. Yang'anirani 28
kwa inu noka, ndi kwa gulu lonse, m' lomwe Nzimu Woyera
unapanga inu oyang'anira, ku busa eklesia la Mulungu,
lomwe anagula ndi mwazi watshi. Didziwa kuti pambuiu 29
kumuka kwanga zirombo zosautsa zidzaloa mwa inu, sikwi-
anja gulu; ndimo kwa inu noka antu adzauka, kulankula 30

zintu zokanika, ku sotsheza akupunzira pambuiu pao.
31 Mwa kuti tshenjerani, kukumbukila kuti ndi ntawi ya dzaka
dzitatu sindinaleka ku ambirira onse usiku ndi usana ndi
32 misozi. Ndimo tsopano dibvomereza inu kwa Mulungu, ndi
kwa mau a kufatsa kwatshi, omwe ali ndi mpamvu ku
manga *inu*, ndi ku patsa *inu* kuloa mwa awo onse omwe ali
33 oyeretsedwa. Sindinasinjirira ndi silivere, kapena golide,
34 kapena miinjiro za muntu modzi. Mudziwa inu noka kuti
manja amene naimirira kwa zofunidwa zanga, ndi kwa awo
35 omwe anali ndi ine. M' zintu zonse dinakupatsani sonyezo,
bwanje kuti kutshita tshointshi mukanatangata ofoka, ndi
ku kumbukila mau a Mwini Yesu, bwanje ie eka nati,
Tshiri tshodala ku patsa kopambana ku landira.
36 Ndimo ntawi ananena tshointshi, nagwada pansi, nape-
37 mpera ndi awo onse. Ndimo awo onse analira kwambiri
38 misozi, nagwa pa kosi la Paulos, namsomsona, kumva
tshisoni kopambana kwa mau omwe ananena, kuti sakaona
nkope yatshi ntawi ina. Ndimo naperekeza ie pa njira
yatshi ku tshombo.
21 Ndimo ntawi kunali kuti tinalekana kwa awo, ndimo
tinaenda ndi matanga, tinafika ndi kupita kolungama kwa
Kos, ndi siku lotsata kwa Rodo, ndi kwa uko ku Patara:
2 ndimo tinapeza tshombo kuyambuka ku Fenike, tinaloa,
3 ndimo tinaenda ndi matanga. Ndimo ntawi tinafika m'
kuona kwa Kipro, kutshisia pa dzanja lamanzere, tinaenda
ndi matanga ku Siriya, naturuka pa Tire: kuti apo tshombo
4 tshinali ku turutsa katundu watshi. Ndimo tinapeza aku-
punzira, tinakala apo masiku asanu ndi awiri: ndimo
amenewa nanena ndi Paulos mwa Nzimu, kuti sakaika pazi
5 m' Yerusalem. Ndimo ntawi kunali kuti tinata masiku,
tinamuka napita ulendo watu; ndimo awo onse, ndi akazi
ndi ana, naperekeza ife pa njira yatu, kwa ntawi tinaturuka
mwa mzinda: ndimo kugwada pa doko, tinapempera, ntina-
6 tsazikana; ndimo tinaloa m' tshombo, koma anabwera kwao
onso.
7 Ndimo ntawi tinamariza ulendo wa nyanja kwa Tire,
tinafika ku Tolimayis; ndimo tinautsa abali, nakala nao
8 siku limodzi. Ndimo pa mawa tinamuka, nafika ku Kesa-
reya: ndi kuloa m' nyumba ya Filipu waivangeli, emwe
9 anali modzi wa asanu ndi awiri, tinakala ndi ie. Ndimo mu-
ntu amene anali ndi ana akazi anai, ziweta, zomwe zinalosa.
10 Ndimo monga tinakala apo masiku ambiri, natsika kwa

Yudeya mprofeti modzi, atshedwa Agabo. Ndimo kufika 11
kwa ife, ndi kutenga lamba la Paulos, namanga mapazi atshi
ndi manja, nati, Tshointsho unena Nzimu Woyera, Tshoi-
ntshi Ayuda pa Yerusalem adzamanga muntu emwe ali
mwini wa lamba limene, nadzapereka ie m' manja a Mitundu.
Ndimo ntawi tinamva zintu zimene, ife ndi awo a malo 12
adya tinapempa ie si ku kwera ku Yerusalem. Ndimo 13
Paulos naiang'ka, Mutshita tshiani, kulira nsozi ndi kuswa
ntima wanga? kuti dirikuta si ku mangidwa koka, koma
anso ku fa pa Yerusalem kwa dzina la Mwini Yesu. Ndimo 14
ntawi sanganakantshiziridwa, tinaleka, kunena, Kufuna kwa
Mwini kutshitidwa.

Ndimo pambuiu masiku amene tinatukula matumba atu, 15
nakwera ku Yerusalem. Ndimo namuka ndi ife enso aku- 16
punzira *ena* kwa Kesareya, kutenga *ndi awo* modzi Mnaso
wa Kipro, wopunzira wamsanga, ndi emwe tikakala.

Ndimo ntawi tinafika ku Yerusalem, abali analandira ife 17
kosekera. Ndimo siku lotsata Paulos naloa ndi ife kwa 18
Yakobi; ndi akuru onse anali apo. Ndimo ntawi anautsa 19
awo, nauza anso tshimodzi ndi tshimodzi zintu zomwe Mulu-
ngu anazitshita mwa Mitundu ndi kuimirira kwatshi. Ndimo 20
awo, ntawi anamva, napambanitsa Mulungu; ndimo nanena
nai', Uona, mbali, bwanje mazousan ambiri alipo mwa Ayuda
a awo omwe anamvana; ndimo ali onse atshitsanzo kwa mau:
ndimo anauzidwa ndi iwe, kuti upunzitsa Ayuda onse omwe 21
ali mwa Mitundu ku sia Moses, kuuza awo sikudula ana ao,
kapena si ku enda pambuiu pa makalidwe. Ndimo tshiri 22
tshiani? adzamva nditu kuti wafika. Ndimo utshite tshimene 23
tshomwe tinena ndi iwe: Tiri ndi antu anai omwe apotshera
kulumbira pa awo; tenga amene, nudzisambitsa ndi awo, 24
nulipira kwa awo, kuti angometa mitu yao: ndimo onse
adzadziwa kuti kulibe nteradi m' zintu ndi zomwe anauzidwa
ndi iwe; koma kuti iwe eka anso upita bwino, kusunga mau.
Koma monga ndi Mitundu yomwe inamvana, tinalemba, 25
kupatsa kuweruza kuti ikanasunga iwo yoka kwa zintu
zinatiridwa kwa mafano, ndi kwa mwazi, ndi kwa tshomwe
tshikwiipidwa, ndi kwa dama. Ndimo Paulos natenga 26
antu, ndi dzua lina kudzisambitsa ndi awo naloa m' tempile,
kuuza kudzaza kwa masiku a kusambitsa, kwa ntawi tshau-
lere tshinatiridwa kwa awo onse.

Ndimo ntawi masiku asanu ndi awiri anali pafupi ku ta, 27
Ayuda kwa Asiya, ntawi anamona m' tempile, nafulumiza

28 antu ambiri onse, naika manja pa ie, kupfula, Amuna, Asira-
yeli, tangatani: Amene ali muntu, emwe apunzitsa antu
onse m' malo onse pa antu, ndi pa mau, ndi malo amene:
ndi kopambana natenga Agrike enso m' tempile, ndimo
29 wadetsa malo oyera amene. Kuti patsogolo anaona ndi ie
muzinda Trofimo Mfeso, emwe naganizaganiza kuti Paulos
30 anatenga m' tempile. Ndimo mzinda wonse unasuntidwa,
ndi antu natamanga pa modzi: ndimo nagwira Paulos, na-
koka ie kwa tempile: ndimo tsopano lino dzitseko dzinatse-
31 kedwa. Ndimo monga analikufuna ku pa ie, makalidwe
anafika kwa kazembe wang'kuru wa gulu, kuti Yerusalem
32 wonse unali m' pokoso. Ndimo tsopano lino natenga ankho-
ndo ndi akenturione, natamanga pa awo: ndimo awo, ntawi
naona kazembe wang'kuru ndi ankhondo, naleka ku menya
33 Paulos. Pomwe kazembe wang'kuru nayandika, namgwira,
nauza ie ku mangidwa ndi maunyolo awiri; nafunsa anali
34 ani, ndi tshomwe anatshita. Ndi ena napfula tshintu tshi-
modzi, ena tshina, mwa antu ambiri: ndimo ntawi sanadziwa
ku dziwa nteradi kwa pokoso, nauza ie ku tengedwa m
35 nyumba ya nkondo. Ndimo ntawi nafika pa makwerero,
kunali tshointsho, kuti ananyamulidwa ndi ankhondo tshi-
36 fuka tsha kukakamiza kwa antu ambiri; kuti antu ambiri
natsata pambuiu, kupfula, Tshotsani ie.

37 Ndimo monga Paulos anatofuna ku tengedwa m' nyumba
ya nkondo, anena ndi kazembe wang'kuru, Kodi dingonena
kantu kwa iwe? Ndimo nati, Kodi udziwa Tshigrike?
38 Kodi suli pomwe Myiputa, emwe patsogolo masiku amene
nafulumiza kupinduka natsogolera m' tshipululu antu mazou-
39 san anai a Ambanda? Koma Paulos nanena, Diri Myuda,
wa Tarso wa Kilikiya, wanzinda wa mzinda si wang'ono:
40 ndimo dipempa iwe, leka ine ku lankula ndi antu. Ndimo
ntawi analoleza, Paulos, kuima pa makwerero, nakodola ndi
dzanja kwa antu; ndimo ntawi kunapangidwa kutontola
kwambiri, nanena nao m' mau a Tshihebere, kuti,

22 Amuna, abali, ndi atate, imvani kudzikana kwanga komwe
tsopano dipanga kwa inu.

2 Ndimo ntawi anamva kuti nanena nao m' mau a Tshihe-
bere, anatontola kopambana: ndimo ati,

3 Diri Myuda, dabadwa m' Tarso wa Kilikiya, koma dale-
redwa m' mzinda umene, pa mapazi a Gamaliyeli, wopunzi-
tsidwa ndi makalidwe olimba a mau a atatu atu, diri watshi-
tsanzo kwa Mulungu, inde monga inu nonse muli m' siku

limene: ndimo dinazunza Njira imene kwa imfa, kumanga 4
ndi kupereka m' nyumba za ndima antu ndi akazi.
Monga anso ndzukuru wang'kuru amariza ndi ine, ndimo 5
makalidwe onse a akuru: kwa omwe enso dinalandira ma-
epistola kwa abali, ndinaenda ulendo kwa Damasko, ku
tenga awo onso omwe anali apo ku Yerusalem m' zomangira,
ku langidwa. Ndimo kunali, kuti, monga dinaenda ulendo 6
wanga, ndinayandika kwa Damasko, pa usana, pompo lino
kunawala kwa kumwamba kuunika kwakukuru ku zungulira
ine. Ndimo dinagwa pansi, ndinamva liu kunena ndi ine, 7
Saulos, Saulos, uzunza ine bwanje? Ndimo dinaiang'ka, 8
Uli ani, Mwini? Ndimo nanena ndi ine, Diri Yesu wa
Nazarete, emwe uzunza. Ndimo awo omwe anali ndi ine 9
naona kuunika nditu, koma sanamva liu la ie emwe nala-
nkula ndi ine. Ndimo dinanena, Didzatshita tshiani, Mwini? 10
Ndimo Mwini nanena ndi ine, Uka, nuloa m' Damasko;
ndimo umo kudzalankulidwa ndi iwe ndi zintu zonse zomwe
zisonyezedwa kwa iwe ku tshita. Ndimo ntawi sindinadzi- 11
wa ku ona kwa kupambana kwa kuunika kumene, kutsogo-
zedwa ndi dzanja la awo omwe anali ndi ine, dinafika m'
Damasko. Ndimo modzi Hananiya, muntu wopembedza kwa 12
mau, wouzidwa bwino ndi Ayuda onse omwe nakala umo,
nafika kwa ine, ndi kuima pafupi ndi ine nanena ndi ine, 13
Mbali Saulos, landira kuona kwako. Ndimo m' ora limeneli
dinayang'ana pa ie. Ndimo nati, Mulungu wa atatu atu 14
waloeza iwe ku dziwa kufuna kwatshi, ndi ku ona Wodeka,
ndi ku mva liu kwa nkamwa mwatshi. Kuti udzamariza 15
ndi ie kwa antu onse ndi tshomwe unaona ndi unamva.
Ndimo tsopano ukala bwanje? uka, nubapatizidwa, nutsuka 16
zakwaipa zako, kuitana pa dzina latshi. Ndimo kunali, 17
kuti, ntawi dinabwera ku Yerusalem, ndimo ntawi dinape-
mpera m' tempile, dinagwa m' tshoona, ndinaona ie kunena 18
kwa ine, Fulumiza, nutshoka nsanga kwa Yerusalem: tshi-
fuka sadzalandira kwa iwe kumariza ndi ine. Ndimo 19
dinanena, Mwini, awo oka adziwa kuti dinaika m' nyumba
ya ndima ndinamenya m' masinagoge onse awo omwe ana-
mvana ndi iwe: ndimo ntawi mwazi wa Stefano womariza 20
wako unaturutsidwa, ine enso dinaima pafupi, ndi kulola,
ndi kusunga miinjiro ya awo omwe anapa ie. Ndimo nanena 21
ndi ine, Muka: kuti didzatumiza iwe kutali kwa Mitundu.

Ndimo napatsa ie kumva kwa mau amene; ndimo 22
natukula mau ao, nati, Tshotsa muntu wotere kwa dziko:

23 kuti sikuenera kuti akale ndi moyo. Ndimo monga na-
pfula, naponya miinjiro yao, natsira fumbi m' mlengalenga,
24 kazembe wang'kuru nauza ie ku tengedwa m' nyumba ya
nkondo, kuuza kuti akafunsidwa ndi kukwapula, kuti
anangodziwa kwa tshifukwa tshiani napfula tshointshi pa ie.
25 Ndimo ntawi anammanga ndi zinsinga, Paulos nanena ndi
kenturione emwe naima pafupi, Kodi tshiri tshamau kwa inu
ku kwapula muntu emwe ali Mroma, ndi wosasutsidwa?
26 Ndimo ntawi kenturione anatshimva, namuka ku kazembe
wang'kuru, nauza ie, kuti, Utofuna ku tshita tshiani? kuti
27 muntu amene ali Mroma. Ndimo kazembe wang'kuru
nafika, nanena nai', Uza ine, kodi uli Mroma? Ndimo
28 nanena, Inde. Ndimo kazembe wang'kuru naiang'ka, Ndi
ndrama zambiri dinalandira unzinda umene. Ndimo
29 Paulos nati, Koma dabadwa *Mroma.* Ndimo awo omwe
anatofunsa ie tsopano lino natshoka kwa ie: ndi kazembe
wang'kuru unso anaopa, ntawi nadziwa kuti anali Mroma,
ndi tshifuka anammanga.
30 Koma pa mawa, kufuna ku dziwa nteradi, mwa kuti
anatshulidwa ndi Ayuda, namasula ie, nauza adzukuru
akuru ndi gulu lonse la ankoswe ku song'kana, natsitsa
Paulos, naika ie patsogolo pa awo.
23 Ndimo Paulos, kuyang'anitsa pa gulu la ankoswe, nati,
Amuna, abali, dinakala ndi moyo patsogolo pa Mulungu m'
2 kudzidziwitsa kwabwino konse kwa siku limene. Ndimo
ndzukuru wang'kuru Hananiya nauza awo omwe naima
3 pafupi ndi ie ku menya ie pa nkamwa. Pomwe Paulos
nanena nai', Mulungu adzamenya iwe, koma loyeretswa iwe:
ndimo kodi ukala ku weruza ine ndi mau, nuuza ine ku
4 menyedwa pa mau? Ndimo awo omwe naima pafupi nati,
5 Kodi unyoza ndzukuru wang'kuru wa Mulungu? Ndimo
Paulos nanena, Sindadziwa, abali, kuti anali ndzukuru wang'-
kuru: kuti alembedwa, Usadzanena tshoipa ndi woweruza wa
6 antu ako. Koma ntawi Paulos nadziwitsa kuti pande limodzi
linali Asadusi, ndi lina Afarisi, napfula m' gulu la ankoswe,
Amuna, abali, diri Mfarisi, mwana wa Afarisi: ndi kulingalira
7 ndi kuukirira kwa akufa diri mfunso. Ndimo ntawi ananena
tshointshi, kunauka kukanirana pakati pa Afarisi ndi Asadusi:
8 ndi kusong'kana kunagawidwa. Kuti Asadusi anena kuti
palibe kuukirira, kapena njelo, kapena nzimu: koma Afarisi
9 abvomera zonse. Ndimo kunauka pokoso lalikuru: ndi ena
a akulembera a pande la Afarisi naima, natetana, kuti,

Sitipeza tshimo m' muntu amene: ndimo tshiani ngati nzimu
unalankula nai', kapena njelo? Ndimo ntawi kanauka 10
kukanirana kwakukuru, kazembe wang'kuru, kuopa kani
Paulos akakadzulidwa ndi awo, nauza ankhondo ku tsika
ndi ku tenga ie ndi mpamvu kwa awo, namtenga m' nyumba
ya nkondo.

Ndimo siku lotsata Mwini naima pafupi ndi ie, nati, Kala 11
wosekera: kuti monga unamariza ndi ine pa Yerusalem,
tshointshi inso ukanamariza ndi ine pa Roma.

Ndimo ntawi unali msana, Ayuda napangana, nadzimanga 12
pansi pa tukwano, kunena kuti kapena sakadia kapena ku
mwa kwa ntawi anapa Paulos. Ndimo anali opambana 13
makumi anai omwe anapanga kunje limene. Ndimo nafika 14
kwa adzukuru akuru ndi akuru, nati, Tinadzimanga pansi
pa tukwano lalikuru, si ku lawa kantu kwa ntawi tapa
Paulos. Ndimo tsopano inu ndi gulu la ankoswe musonyeza 15
ku kazembe wang'kuru kuti angotenga ie kwa inu, monga
ngati mukaweruza mrandu watshi koyang'anira kopambana:
ndimo ife, patsogolo ie afika pafupi, tirikuta kumpa. Koma 16
mwana wa mlongo wa Paulos anamva ndi kubisalira kwao,
ndimo nafika naloa m' nyumba ya nkondo, nauza Paulos.
Ndimo Paulos naitana kwa ie modzi wa akenturione, nati, 17
Tenga nyamata amene kwa kazembe wang'kuru: kuti ali
ndi kantu ku uza ie. Ndimo nagwira ie, namtenga ku 18
kazembe wang'kuru, ndimo ati, Paulos womangidwa naitana
ine kwa ie, nafunsa ine ku tenga nyamata amene kwa iwe,
emwe ali ndi kantu ku lankula ndi iwe. Ndimo kazembe 19
wang'kuru natenga ie ndi dzanja, ndimo kupita kutseri
namfunsa, Tshimene tshiri tshiani tshomwe uli natsho ku
uza ine? Ndimo nati, Ayuda anagwirizana ku funsa iwe 20
ku tsitsa Paulos mawa kwa gulu la ankoswe, monga ngati
ukafunsa kantu koyang'anira kopambana ndi ie. Ndimo 21
usabvomera awo: kuti anabisalira kwa ie a awo opambana
makumi anai a antu, omwe anadzimanga pansi pa tukwano,
kapena si ku dia kapena ku mwa kwa ntawi anampa: ndimo
tsopano ata, kuyang'anira kwa kulonjezana kwa iwe.
Ndimo kazembe wang'kuru naleka nyamata ku muka, 22
kuuza ie, Usauza muntu modzi kuti wasonyeza zintu
zimenezi kwa ine. Ndimo naitana kwa ie awiri a akentu- 23
rione, nati, Konzetsani ankhondo mazana awiri ku enda
monga kutali monga Kesareya, ndi antu apakavalo makumi
asanu ndi awiri, ndi antungo mazana awiri, pa ora latshitatu

24 la usiku: ndimo *nauza awo* ku kwanitsa nyama, kuti
anangoika Paulos pa izo, natenga ie wopulumuka ku
25 Felikis woweruza. Ndimo nalemba epistola pambuiu
makalidwe amene:
26 Klaudiyo Lisiya kwa woweruza wabwino wopambana
27 Felikis, kuutsa. Muntu amene anagwidwa ndi Ayuda, ndi
anatofuna ku pedwa ndi awo, ntawi dinafika pa awo ndi
ankhondo, napulumutsa ie, kunadziwa kuti anali Mroma.
28 Ndimo kufuna kudziwa tshifukwa ndi tshomwe natshula ie,
29 dinatsitsa ie ku gulu la ankoswe lao: emwe dinapeza ku
tshulidwa ndi mafunso a mau ao, koma ku potshera palibe
kantu koenera kwa imfa kapena kwa zomanga kanaikidwa
30 pa ie. Ndimo ntawi kunasonyezedwa kwa ine kuti kunje
likakala pa muntu, dinamtumiza kwa iwe tsopano lino,
kuuza akutshula atshi inso ku nena pa ie patsogolo pa
iwe.
31 Ndimo ankhondo, monga kunauzidwa awo, nagwira
32 Paulos, namtenga usiku ku Antipatris. Koma pa mawa
nasia apakavalo ku enda ndi ie, nabwera ku nyumba ya
33 nkondo: ndimo awo, ntawi nafika ku Kesareya, napereka
epistola kwa woweruza, naika Paulos anso patsogolo pa ie.
34 Ndimo ntawi analiwerenga, nafunsa ndi kadziko kati anali;
35 ndimo ntawi anadziwa kuti anali wa Kilikiya, Didzamva
mrandu wako, nati, ntawi akutshula ako onso anafika:
ndimo nauza ie ku sungidwa m' Pretorium la Herode.

24 Ndimo pambuiu masiku asanu ndzukuru wang'kuru
Hananiya natsika ndi akuru ena, ndimo *ndi* wogwira-moyo,
modzi Tertulo; ndimo nataulira woweruza pa Paulos.
2 Ndimo ntawi anaitanidwa, Tertulo naamba ku tshula ie,
kuti,
Kuona kuti ndi iwe tisekera ntendere wambiri, ndimo
kuti ndi mwa kuganiza-patsogolo kwako zoipa zifotokozedwa
3 kwa mtundu umene, tiulandira mwa njira zonse ndi m' malo
onse, Felikis wabwino wopambana, ndi kuyamika konse.
4 Koma, kuti sindikala wotshedwa wopambana kwa iwe,
dipempa iwe ku mva ife ndi kuyanja kwako mau owereng'-
5 jeka. Kuti tinapeza muntu amene muntu wobvuta, ndi
wosunta wa mauko mwa Ayuda onse mwa dziko, ndimo
6 tsatsogolo wa kugawa kwa Anazarete: emwe kopambana
8 anayesa ku ipitsa tempile: pa emwe enso tinagwira: kwa
emwe udzadziwa, ndi kumfunsira iwe eka, ku dziwitsa ndi
9 zintu zonse zimenezi, ndi zomwe titshula ie. Ndimo Ayuda

anso nadzipatika m' tshulo, kubvomera kuti zintu zimenezi zinali tshointsho.

Ndimo ntawi woweruza anakodola ie ku nena, Paulos 10
naiang'ka,

Mwa kuti didziwa kuti unakala kwa dzaka dzambiri
woweruza kwa mtundu umene, dipanga kudzikana kwanga
kosekera: kuona kuti udziwa ku dziwitsa, kuti kusali kopa- 11
mbana masiku kumi ndi awiri kwa ntawi dinakwera ku Yeru-
salem ku pembedza: ndimo kapena m' tempile sanapeza ine 12
kugazitsana ndi muntu modzi kapena kufulumiza antu ambiri,
kapena m' masinagoge, kapena m' mzinda. Kapena osadziwa 13
ku limbitsa kwa iwe zintu ndi zomwe tsopano atshula ine.
Koma tshimene dibvomera kwa iwe, kuti pambuiu Njira 14
yomwe atsha kugawa, tshointsho diimirira Mulungu wa atatu
atu, kumvana zintu zonse zomwe ziri kwamau, ndi zomwe
zilembedwa mwa aprofeti: kuli ndi kulingalira kwa 15
Mulungu, komwe amene enso awo oka ayang'anira, kuti
kudzali kuukirira kwa odeka ndi kwa osadeka. Mwa 16
kuti inso didziyesa ku potshera kudzidziwitsa kopanda
tshimo kwa Mulungu ndi antu ntawi yonse. Ndimo pa- 17
mbuiu dzaka dzambiri dinadza ku tenga zaulere kwa
mtundu wanga, ndi zotsira: mwa zimene nandipeza 18
wosambitsidwa m' tempile, wopanda antu ambiri, kapena
kosuntira si ndi pokoso: koma *anali* Ayuda ena kwa
Asiya—omwe akanakala kuno patsogolo pa iwe, ndi ku 19
panga tshulo, ngati anali ndi kantu pa ine. Kapena anso 20
antu amene awo oka atshule tshimo lomwe anapeza, ntawi
dinaima patsogolo gulu la ankoswe, kani kudzali kwa liu 21
limodzi limene, lomwe dinapfula kuima mwa awo, Ndi
kuukirira kwa akufa diri mfunso patsogolo pa inu siku
limeneli.

Koma Felikis, ali ndi kudziwa kwakudziwitsa kopambana 22
ndi Njira, natshedwetsa awo, kuti, Ntawi Lisiya kazembe
wang'kuru adzatsika, didzamariza mrandu wanu. Ndimo 23
nauza kenturione kuti akasungidwa m' kudikira, ndimo
akakala ndi kuyanja; ndimo si ku letsa modzi wa abali
atshi ku imirira kwa ie.

Koma pambuiu masiku ena, Felikis nafika ndi Drusila, 24
nkazi watshi, emwe anali Myuda wankazi, natumizira
Paulos, namva ie ndi mvanu m' Kristu Yesu. Ndimo 25
monga nagazitsana ndi kudeka, ndi kudziweruza, ndi
kuweruza ku dza, Felikis anaopsedwa, naiang'ka, Muka kwa

ntawi imene; ndimo ntawi diri ndi nsiku yabwino, didzai-
26 tana iwe kwa ine. Analingalira nditu kuti ndrama
zikapatsidwa kwa ie ndi Paulos: mwa kuti inso natumizira
27 ie kawiri kawiri, nalankula nai'. Koma ntawi dzaka dziwiri
dzinadzazidwa, Felikis analoezedwa ndi Porkiyo Festo; ndi
kufuna ku peza kuanja ndi Ayuda, Felikis nasia Paulos m'
zomangira.

25 Ndimo Festo, kunafika pa kadziko, pambuiu masiku atatu
2 nakwera ku Yerusalem kwa Kesareya. Ndimo adzukuru
akuru ndi antu akuru a Ayuda anataulira ie pa Paulos:
3 ndimo napempa ie, kufunsa kuanja pa ie, kuti akatumizira ie
4 ku Yerusalem; kubisalira ku pa ie pa njira. Koma Festo
naiang'ka, kuti Paulos anasungidwa m' kudikira pa Kesareya,
5 ndi kuti ie eka anatofuna ku tshoka nsanga *uko.* Ndimo
awo, ati, omwe ali ndi mpamvu mwa inu atsike ndi ine,
ndimo ngati kuli kantu katshimo m' muntu, awo atshule
ie.

6 Ndimo ntawi anakala mwa awo si kopambana masiku
asanu ndi atatu kapena kumi, natsika ku Kesareya; ndi pa
mawa nakala pa mpando woweruza, nauza Paulos ku
7 tengedwa. Ndimo ntawi anafika, Ayuda omwe anatsika
kwa Yerusalem naima ozungulira ie, ku tshula pa ie matshulo
8 ambiri ndi olemera, omwe sanadziwa ku limbitsa; ntawi
Paulos nati m' kudzikana kwatshi, Kapena si pa mau a
Ayuda, kapena pa tempile, kapena pa Kesare, sadatshimwa
9 konse. Koma Festo, kufuna ku peza kuanja ndi Ayuda,
naiang'ka Paulos, nati, Kodi udzakwera ku Yerusalem, ndi
apo ku weruzidwa ndi zintu zimenezi patsogolo pa ine?
10 Koma Paulos nati, Dirikuima patsogolo pa mpando wowe-
ruza wa Kesare, pomwe dikanaweruzidwa: kwa Ayuda
datshita palibe tshimo, monga iwe enso udziwa bwino nditu.
11 Ndimo ngati diri wotshita zoipa, ndimo datshita kantu
koenera kwa imfa, sindikana ku fa: koma ngati palibe
tshimodzi tsha zintu zimenezi tshiri *tshoona,* ndi zomwe
amene atshula ine, palibe muntu adziwa ku pereka ine kwa
12 awo. Dilekera kwa Kesare. Ndimo Festo, ntawi anauzana
ndi gulu la ankoswe, naiang'ka, Walekera kwa Kesare: kwa
Kesare udzamuka.

13 Ndimo ntawi masiku ena anapita, Agripa fumu yotshuka
14 ndi Bernike nafika pa Kesareya, nautsa Festo. Ndimo
monga nakala apo masiku ambiri, Festo naika mrandu wa
Paulos patsogolo fumu yotshuka, kuti, Kuli muntu modzi

nasiidwa womangidwa ndi Felikis: ndi emwe, ntawi dinali 15
pa Yerusalem, adzukuru akuru ndi akuru a Ayuda nataulira
*ine*, kufunsa kwa kumariza pa ie. Kwa omwe dinaiang'ka, 16
kuti sikuli makalidwe a Aroma ku pereka muntu modzi,
patsogolo kuti wotshulidwa apotshera otshula nkope ndi
nkope, napotshera pofatsa ku panga kudzikana kwatshi ndi
tshulo linaikidwa pa ie. Ndimo ntawi anasong'kana pano, 17
sindinatshedwa, koma pa siku lina dinakala pa mpando
woweruza, nauza muntu ku tengedwa. Ndi emwe, ntawi 18
otshula naima, sanatenga tshulo limodzi la zintu zoipa zotere
monga dinaganizaganiza; koma anali ndi mafunso ena pa ie 19
ndi kupembedza kwao, ndimo ndi modzi Yesu, emwe anafa,
emwe Paulos anatshimika ku li wamoyo. Ndimo ine, dinadzi- 20
sing'kasing'ka bwanje ku funsira ndi zintu zimenezi, dina-
funsa ngati akaenda ku Yerusalem, ndimo apo ku weruzidwa
ndi mirandu imene. Koma ntawi Paulos analekera ku 21
sungidwa kwa kumariza kwa Sebasto, dinauza ie ku sungi-
dwa kwa ntawi dikatumiza ie kwa Kesare. Ndimo Agripa 22
*nanena* ndi Festo, Dinalikufuna anso ine ndeka ku mva
muntu. Mawa, ati, udzamva ie.

Ndimo pa mawa, ntawi Agripa anafika, ndi Bernike, ndi 23
kuyerekera kwakukuru, ndimo analoa m' malo a kumva, ndi
akazembe akuru, ndi amuna akuru a mzinda, pa kuuza kwa
Festo Paulos naloezwa. Ndimo Festo ati, Fumu Yotshuka 24
Agripa, ndi amuna onse omwe ali pano ndi ife, muona muntu
amene, ndi emwe antu ambiri onse a Ayuda anapanga
mrandu kwa ine, pa Yerusalem ndi pano, kupfula kuti
sakanakala ndi moyo ntawi ina. Koma dinapeza kuti 25
sanatshita kantu koenera kwa imfa: ndimo monga ie eka
analekera kwa Sebasto dinayerekeza ku tumiza ie. Ndi emwe 26
sindipotshera kantu kolimba ku lemba ku mwini wanga.
Ndimo damturutsa patsogolo pa inu, ndi kopambana patsogolo
pa iwe, fumu yotshuka Agripa, kuti, pambuiu kufunsa
kunatshitidwa, dingopotshera kantu ku lemba. Kuti 27
tshionedwa kwa ine kopanda dingalira, m' kutumiza
womangidwa, si inso ku sonya matshulo pa ie.

Ndimo Agripa nanena ndi Paulos, Uloledwa ku nena kwa 26
iwe eka. Ndimo Paulos naturutsa dzanja latshi, napanga
kudzikana kwatshi:

Diganiza ine ndeka wosekera, fumu yotshuka Agripa, 2
kuti dirikupanga kudzikana kwanga patsogolo pa iwe
siku limene ndi zintu zonse ndi zomwe ditshulidwa ndi

3 Ayuda: kopambana tshifuka uli wanzeru ndi makalidwe
onse ndi mafunso zomwe ziri mwa Ayuda: mwa kuti
4 dipempa iwe ku mva ine kolongosola. Ndimo makalidwe
anga a moyo kwa ubwana wanga, womwe unali kwa kuamba
mwa mtundu wanga, ndi pa Yerusalem, Ayuda onse
5 adziwa; kupotshera kudziwa kwa ine kwa kuamba, ngati
afuna ku mariza, bwanje kuti pambuiu kugawa kolimba
kopambana kwa kupembedza kwatu dinakala ndi moyo
6 Mfarisi. Ndimo tsopano diima *pano* ku weruzidwa kwa
kulingalira kwa kulonjezana kunapangidwa ndi Mulungu
7 kwa atatu atu; ndi kwa *kulonjezana* kumene mafuko kumi
ndi awiri atu, kuimirira *Mulungu* kolimba usiku ndi msana,
alingalira ku fika. Ndimo ndi kulingalira kumene ditshuli-
8 dwa ndi Ayuda, O fumu yotshuka! Bwanje tshiweruzidwa
9 kosamvana ndi inu, ngati Mulungu aukitsa akufa? Dina-
ganiza nditu ndine ndeka, kuti dikanatshita zintu zambiri
10 pa dzina la Yesu wa Nazarete. Ndimo tshimene enso
dinatshita m' Yerusalem: ndimo dinatsekera ambiri a oyera
m' nyumba za ndima, kunalandira kuweruza kwa adzukuru
akuru, ndimo ntawi anaikidwa kwa imfa, dapatsa funo langa
11 pa awo. Ndi kulanga awo ntawi zambiri m' masinagoge
onse, dinayesa ku panga awo ku tukwana; ndimo dinali-
kukwia kwambiri pa awo, dinazunza awo inde kwa mizinda
12 ya dziko lina. Mwa kuti monga dinaenda ulendo ku
Damasko ndi kuweruza ndi kuuza kwa adzukuru akuru,
13 pa usana, O fumu yotshuka, dinaona pa njira kuunika
kwa kumwamba, kopambana kuwala kwa dzua, kuwala
kozunguniza ine ndi awo omwe naenda ulendo ndi ine.
14 Ndimo ntawi ife tonse tinagwa pansi, dinamva liu kunena
ndi ine m' liu la Tshihebere, Saulos, Saulos, bwanje uzunza
ine? tshiri tsholimba kwa iwe ku kang'ka pa zofulumizira.
15 Ndimo dinanena, Uli ani, Mwini? Ndimo Mwini nati, Diri
16 Yesu emwe uzunza. Koma uka, nuima pa mapazi ako:
kuti kwa nsonga imene dadzisonyeza kwa iwe, ku loeza iwe
woimirira ndi womariza a zintu mwa zomwe wandiona, ndi
17 a zintu mwa zomwe didzadzisonyeza kwa iwe; kupulumutsa
iwe kwa antu, ndi kwa Mitundu, kwa yomwe ditumiza iwe,
18 ku tsegula maso ao, kuti ingotembenuka kwa ndima kwa
kuunika, ndi kwa mpamvu ya Satana ku Mulungu, kuti
ingolandira kubweza kwa zakwaipa ndi kuloa mwa awo
19 omwe ayeretsedwa ndi mvanu mwa ine. Mwa kuti, O fumu
yotshuka Agripa, sindinali wosamvera kwa tshoona

tshakumwamba: koma dinauza kwa awo a Damasko ku- 20
amba, ndi pa Yerusalem, ndi mwa dziko lonse la Yudeya,
ndi inso kwa Mitundu, kuti akatembenuza ntima natembe-
nuka ku Mulungu, ku tshita ntshito zoenera za kutembenuza
ntima. Kwa tshifukwa tshimene Ayuda nagwira ine m' 21
tempile, nayesa kundipa. Ndimo dinalandira kutangata 22
komwe kuli kwa Mulungu, diima kwa siku limene kumariza
kwa ang'ono ndi akuru, kunena tshabe koma tshomwe
aprofeti ndi Moses analankula tshikafika; bwanje kuti 23
Kristu akanamva, *ndi* bwanje kuti poiamba ndi kuukirira
kwa akufa akauza kuunika kwa antu ndi kwa Mitundu.

Ndimo monga tshointsho napanga kudzikana kwatshi, 24
Festo anena ndi liu lalikuru, Paulos, uli wamisala;
kupunzira kwako kwambiri kutembenuza iwe kwa misala.
Koma Paulos ati, Sindiri wamisala, Festo wabwino wopa- 25
mbana; koma diuza mau a nteradi ndi a kudziweruza.
Kuti fumu yotshuka idziwa ndi zintu zimenezi, kwa yomwe 26
enso dilankula kolere: kuti diyerekezedwa kuti palibe
tshimodzi tsha zintu zimenezi tshibisidwa kwa iyo; kuti
tshimene sitshatshitidwa m' ngondia. Fumu Yotshuka 27
Agripa, kodi umvana aprofeti? Didziwa kuti umvana.
Ndimo Agripa *nanena* ndi Paulos, Ndi kakuyerekeza ka- 28
kang'ono ukafuna ku panga ine Mkristu. Ndimo Paulos 29
*nati*, Difuna kwa Mulungu, kuti kapena ndi kang'ono
kapena ndi kwambiri, si iwe eka, koma anso onse omwe
amva ine siku limene, anangokala kotere monga diri, kopanda
zomangira zimenezi.

Ndimo fumu yotshuka inauka, ndi woweruza, ndi 30
Bernike, ndi awo omwe nakala nao: ndimo ntawi anapa- 31
mbuka, nalankula modzi ndi wina, kuti, Muntu amene
atshita palibe kantu koenera kwa imfa kapena kwa zomangira.
Ndimo Agripa nanena ndi Festo, Muntu amene anangomasu- 32
lidwa, ngati sanalekera kwa Kesare.

Ndimo ntawi kunayerekezedwa kuti tikaenda ndi matanga 27
kwa Yitaliya, napereka Paulos ndi omangidwa ena ku
kenturione atshedwa Yuliyo, wa gulu la Sebasto. Ndimo 2
kuloa m' tshombo tsha Adramita, tshomwe tshinatoenda
ndi matanga kwa malo pa doko la Asiya, tinapita ku nyanja,
Aristarko, Wakumakedoniya wa Tesalonika, ali ndi ife.
Ndimo siku lina tinafika pa Tsidon: ndi Yuliyo natshita 3
kokoma ndi Paulos, naloleza ie ku enda ku abali atshi kudzi-
sangalatsa. Ndimo kupita ku nyanja kwa uko, tinaenda 4

ndi matanga m' kudika kwa Kipro, tshifuka mpepo zinali
5 patsogolo. Ndimo ntawi tinadutsa ndi matanga nyanja
yomwe iri pandunji pa Kilikiya ndi Pamfiliya, tinafika ku
6 Mira, *mzinda* wa Likiya. Ndimo apo kenturione napeza
tshombo tsha Alesandria kuenda ndi matanga kwa Yitaliya ;
7 ndimo naika ife momo. Ndimo ntawi tinaenda ndi matanga
kododoma masiku ambiri, ndimo tinafika ndi ntshito yambiri
pandunji pa Kinido, mpepo si ku lola ife kopambana,
tinaenda ndi matanga m' kudika kwa Krete, pandunji pa
8 Salmone ; ndimo ndi ntshito yambiri ndi kulambalala itsho
tinafika kwa malo amodzi atshedwa Mapote Abwino ; pafupi
ndi awo, unali mzinda wa Laseya.
9 Ndimo *pambuiu* ntawi yambiri inapisidwa, ndimo ulendo
wa nyanja unali ndi kutsekerezwa, tshifuka Kuleka kudia
10 kunapita kali, Paulos nataulira awo, nanena nao, Mafumu,
didziwitsa kuti ulendo wa nyanja udzali ndi kupweteka ndi
kumwaza kwambiri, si kwa katundu ndi tshombo zoka, koma
11 anso kwa moyo watu. Koma kenturione nasamala kwambiri
kwa mbuiye ndi kwa mwini wa tshombo, kopambana ndi
12 zintu zimenezo zomwe zinanenedwa ndi Paulos. Ndimo
tshifuka pote losali bwino kukala malimwe momo, unyinji
unataulira ku pita ku nyanja kwa uko, ngati ndi zifukwa
zina akafika kwa Fenikis, nakala malimwe *umo ; lomwe liri*
pote la Krete, kuyang'ana mpoto-bvuma ndi mwela-bvuma.
13 Ndimo ntawi mwela inaomba pang'ono, kuganizaganiza kuti
analandira kuyerekeza kwao, natukula nangula naenda ndi
14 matanga mbali mwa Krete, pafupi ndi gombe. Koma pa-
mbuiu si ntawi yeitali inamenya kwa itsho mpepo yeikuru,
15 yomwe itshedwa Yurakwilo : ndimo ntawi tshombo tshina-
gwidwa, ndimo tshosanadziwa ku loza mpepo, tinadenguma
16 *kwa iyo*, ntinakang'kidwa. Ndimo kutamanga m' kudika
kwa tshisi tshatshing'ono tshitshedwa Kauda, tinali ndi
17 mpamvu, ndi ntshito yambiri, ku limbitsa katshombo : ndi-
mo ntawi anatukula iko, anatshita ndi matangato, ku kola
tshombo ; ndi, kuopa kani akataiikidwa pa Sirtis, natsitsa
18 zintu za tshombo, ndi tshointsho tinakang'kidwa. Ndimo
monga tinalemedwa kwambiri ndi mondwe, dzua lina anaamba
19 ku ponya *katundu* kunja ; ndimo siku latshitatu naturutsa
20 ndi manja ao zintu za tshombo. Ndimo ntawi kapena dzua
kapena nyenyezi sizinawala pa *ife* kwa masiku ambiri, ndimo
si mondwe wang'ono unali pa *ife* kulingalira konse kuti
21 tikapulumutsidwa tsopano kunatshotsedwa. Ndimo ntawi

anakala *ntawi* yeitali opanda kudia, pomwe Paulos anaima
pakati pa awo, nati, Mafumu, mukanamva ine, ndimo simu-
naenda ndi matanga kwa Krete, ndimo simwalandira ku-
pwetekwa kumene ndi kumwaza. Ndimo tsopano ditaulira 22
inu ku kala kosekera: kuti kudzakala palibe kumwaza kwa
moyo mwa inu, koma kwa tshombo *tshoka.* Kuti naima 23
ndi ine usiku umene njelo wa Mulungu wa emwe diri, emwe
enso diimirira, kuti, Usaopa, Paulos; ukanaima patsogolo 24
pa Kesare: ndi ona, Mulungu wapatsa iwe onse awo omwe
aenda ndi matanga ndi iwe. Mwa kuti, mafumu, kalani 25
kosekera: kuti dimvana ndi Mulungu, kuti tshidzakala inde
tshointsho monga tshinalankulidwa ndi ine. Koma tikana- 26
taiidwa pa tshisi tshimodzi.

Koma ntawi usiku kumi ndi watshinai unafika, monga 27
tinakang'kidwa kwina ndi kwina m' *nyanja ya* Adriya, pa
pakati pa usiku amatanga anaganizaganiza kuti analikuya-
ndika ku dziko lina; ndimo nayesa, napeza mikwamba makumi 28
awiri: ndimo pambuiuntawi yeing'ono, nayesa anso, napeza mi-
kwamba kumi ndi isanu. Ndimo kuopa kani nditu tikataiidwa 29
pa gombe pa malo a matantwe, natsitsa anangula anai kwa
makaliro, nafunitsa kwa msana. Ndimo monga amatanga 30
analikufuna ku tawa m' tshombo, ndimo anatsitsa katshombo
m' nyanja, kofana ngati monga afuna ku turutsa anangula pa
likuru, Paulos nanena ndi kenturione ndimo ndi ankhondo, 31
Ngati amene osakala m' tshombo, musadziwa ku pulumutsi-
dwa. Ndimo ankhondo nadula zingwe za katshombo, naleka 32
iko ku gwa. Ndimo ntawi banda kutsha unalinkudza, Paulos 33
napempa awo onse kutenga kantu ka kudia, kuti, Siku limene
liri siku kumi ndi latshinai lomwe mulinda ndi mukalabe
kuleka kudia, simunatenga kantu. Mwa kuti dipempa inu 34
ku tenga kantu kakudia: kuti kumene kuli kwa kupulumuka
kwanu: kuti palibe tsisi limodzi lidzamwazika kwa mutu
wa modzi wa inu. Ndimo ntawi ananena amene, ndimo 35
anatenga nkate, napatsa tshakoma kwa Mulungu patsogolo
pa onse: nauswa, naamba ku dia. Pomwe onse anali ose- 36
kera, ndi awo oka anso natenga kudia. Ndimo tinali ife 37
tonse m' tshombo mizimu mazana awiri, makumi asanu ndi
awiri ndi isanu ndi umodzi. Ndimo ntawi anadia kokwana, 38
napeputsa tshombo, kuturutsa trigu m' nyanja. Ndimo 39
ntawi linali dzua, sanadziwa ntunda: koma naona bondo
limodzi ndi doko, ndimo nagazitsana ngati anadziwa ku
kang'ka tshombo pa ilo. Ndimo kutaia anangula, nasia awo 40

m' nyanja, pa ntawi yomwe kumasula zomangira za matsi-
kiro; ndimo kutukula tanga lapatsogolo kwa mpepo, nafu-
41 na doko. Koma kufika pa nkhumano pa mafundi awiri,
napisa tshombo pa ntunda; ndi likuru la tshombo linamenya
ndi linatsala lopanda ku suntwa, koma makaliro naamba ku
42 sweka ndi mpamvu *ya mafundi*. Ndimo kugazitsana kwa
ankhondo kunali ku pa omangidwa, kani modzi *wa awo*
43 akasambira kunja, ndi ku pulumuka. Koma kenturione,
kufuna ku pulumutsa Paulos, naletsa awo kwa kuyerekeza
kwao; nauza kuti awo omwe nadziwa ku sambira akadzi-
44 ponya kunja, ndi ku fika poiamba pa ntunda: ndimo otsala,
ena pa matabwa, ndi ena pa zintu *zina* kwa tshombo.
Ndimo tshointsho tshinali, kuti awo onse napulumuka bwino
pa ntunda.

28 Ndimo ntawi tinapulumutsidwa, pomwe tinadziwa kuti
2 tshisi tshinatshedwa Melita. Ndimo abaribari nasonyeza ife
kukoma si kwakung'ono: kuti nakoleza moto, nalandira ife
tonse, tshifuka tsha mvula yatsopano, ndi tshifuka tsha
3 kuzizira. Koma ntawi Paulos anasong'kanitsa mtolo wa
kuni, naika izo pa moto, njoka inaturuka tshifuka tsha
4 kutenta, nigwira pa dzanja latshi. Ndimo ntawi abaribari
naona tshirombo ku patshikwa kwa dzanja latshi, nanena
modzi ndi wina, Lopanda ganizo muntu amene ali wa-
mbanda, emwe, ngati wapulumuka kwa nyanja, koma Kudeka
5 kusanalola ku kala ndi moyo. Koma nakang'ka tshirombo
6 m' moto, ndimo sanapwetekwa. Koma nayang'anira kuti
akanatupa, kapena akanagwa wakufa nsangansanga: koma
ntawi anakala ntawi yeitali ndi kuyang'anira, ndimo sanaona
kantu koipa kufika pa ie, nasintanitsa mauongo ao, nanena
kuti anali mulungu.

7 Ndimo pafupi ndi malo amene inali minda ya muntu
wang'kuru wa tshisi, atshedwa Publiyo; emwe nalandira
8 ife, nasunga ife ndi ulemu masiku atatu. Ndimo kunali
tshointsho, kuti atatu atshi a Publiyo anadwala malungo ndi
tshiziula: kwa emwe Paulos naloa, napempera, ndi kuika
9 manja atshi pa ie namtshiritsa. Ndimo ntawi tshimene
tshinatshitidwa, otsala anso omwe anali ndi zintenda m'
10 tshisi anafika, ndimo anatshiritsidwa: omwe enso anatile-
mekeza ndi maulemu ambiri; ndimo ntawi tinaenda ndi
matanga, naika m' tshombo zintu zotere monga tinafuna.

11 Ndimo pambuiu miezi itatu tinaenda ndi matanga m'
tshombo tsha Alesandriya, tshomwe tshinakala malimwe m'

tshisi, tshizindikilo tshatshi tshinali Ana Amamuna a Mpasa.
Ndimo anafika pa Surakus, tinakala apo masiku atatu. 12
Ndimo kwa uko tinapanga kuzungulira, tinafika pa Regiyon: 13
ndimo pambuiu siku limodzi mwela unauka, ndi pa siku
latshiwiri tinafika kwa Puteyoli: pomwe tinapeza abali, 14
ndimo tinafunsidwa ku kala nao masiku asanu ndi awiri:
ndimo tshointsho tinafika kwa Roma. Ndimo kwa uko 15
abali, ntawi anamva ndi ife, nafika ku komana ndi ife monga
kutali monga Malo a Maronda a Apiyo, ndi Mabwalo Atatu:
omwe ntawi Paulos naona, nanena tshakoma kwa Mulungu,
nalimbikitsa ntima watshi.

Ndimo ntawi tinaloa m' Roma, Paulos analolezedwa ku 16
kala ie eka ndi wankhondo emwe nadikira ie.

Ndimo kunali, kuti pambuiu masiku atatu nasong'kanitsa 17
awo omwe anali akuru a Ayuda: ndimo ntawi anasong'kana-
nidwa, nanenanao, Ine, amuna, abali, ngati sindinatshita kantu
pa antu, kapena pa makalidwe a atatu atu, kosuntira dina-
perekedwa womangidwa kwa Yerusalem m' manja a Aroma:
omwe, ntawi anafunsira ine, nafuna ku masula ine, tshifuka 18
kunali palibe tshifukwa tsha imfa mwa ine. Koma ntawi 19
Ayuda nanena pa iko, dinafulumizidwa ku lekera kwa
Kesare; si kuti dinali ndi kantu ku tshula ndi mtundu
wanga. Ndimo kwa tshifukwa tshimene dinaitana inu ku 20
ona ndi ku nena ndi *ine:* kuti tshifuka tsha kulingalira kwa
Sirayeli dimangidwa ndi unyolo umene. Ndimo nanena 21
nao, Sitinalandira kapena maepistola kwa Yudeya ndi iwe,
kapena ena a abali sanafika kuno ku bukitsa kapena ku
lankula kantu ka mpingo ndi iwe. Koma tifuna ku mva 22
kwa iwe tshomwe uganiza: kuti monga kwa kugawa ku-
mene, kudziwidwa ndi ife kuti m' malo onse kunenedwa pa
*iko.*

Ndimo ntawi anaikidwa kwa ie siku limodzi, nafika kwa 23
ie m' kukala kwatshi m' kuwerenga kwakukuru; kwa omwe
nazizika, kumariza dziko la Mulungu, ndi kuyerekeza awo
ndi Yesu, kwa mau a Moses ndi kwa aprofeti, kwa mawa
ndi ndzulo. Ndimo ena namvana ndi zintu zomwe zina- 24
nenedwa, ndi ena sanamvana. Ndimo ntawi sanagwirizana, 25
natshoka, pambuiu kuti Paulos ananena mau amodzi, Bwino
unalankula Nzimu Woyera mwa Yesaya mprofeti kwa atatu
anu, kuti, 26

Muka iwe kwa antu amene, nunena,
Ndi kumva mudzamva, ndimo simunadziwa konse;

Ndimo kuona mudzaona, ndimo simudzadziwitsa konse:
27 Kuti ntima wa antu amene unakulitswa kolemedwa,
Ndi makutu ao ali otseka ku mva,
Ndi maso ao mwatseka;
Kani nditu akaoneka ndi maso ao,
Ndi ku mva ndi makutu ao,
Ndi ku dziwa ndi ntima wao,
Ndimo akatembenuka anso,
Ndikatshiritsa awo.
28 Ndimo kudziwidwa ndi inu, kuti kupulumutsa kumene
kwa Mulungu kutumizidwa kwa Mitundu: iyo onso idza-
mva.
30 Ndimo nakala dzaka dziwiri dzonse m' nyumba yatshi
31 yolipidwa, nalandira onse omwe naloa kwa ie, kuuza dziko
la Mulungu, ndi kupunzitsa zintu ndi Mwini Yesu Kristu
ndi kulimbika ntima konse, palibe modzi kuletsa ie.

---

EPISTOLA LA PAULOS KWA

# AROMA.

1 PAULOS, kapolo wa Yesu Kristu, woitanidwa *ku kala*
2 mpostile, wosang'kidwa kwa ivangeli wa Mulungu,
womwe analonjezana kali mwa aprofeti atshi m' malemba
3 oyera, ndi Mwana watshi, emwe anabadwa kwa mbeu ya
4 Davide ndi nyama, emwe anaikidwa Mwana wa Mulungu
m' mpamvu, ndi nzimu wa kuyera, ndi kuukirira kwa
5 akufa; *inde* Yesu Kristu Mwini watu, mwa emwe tinala-
ndira kufatsa ndi upostile, kwa kumvera kwa mvanu mwa
6 mitundu yonse, kwa dzina latshi: mwa omwe muli inso,
7 aitanidwa *ku kala* a Yesu Kristu: kwa onse omwe akala
m' Roma, okondedwa ndi Mulungu, aitanidwa *ku kala* oyera:
kufatsa kwa inu ndi ntendere kwa Mulungu Atatu atu ndi
Mwini Yesu Kristu.
8 Kuiamba, dinena tshakoma kwa Mulungu wanga mwa
Yesu Kristu kwa inu nonse, tshifuka mvanu wanu uuzidwa

mwa dziko lonse. Kuti Mulungu ali womariza wanga, 9
emwe diimirira munzimuwanga m' ivangeli wa Mwana watshi,
bwanje kosareka dinena ndi inu, ntawi zonse m' mapempero
anga kufunsa, ngati ndi zifukwa zina inde tsopano dingole- 10
mereredwa ndi kufuna kwa Mulungu ku fika kwa inu.
Kuti difunitsa ku ona inu, kuti dingopatsa kwa inu tshau- 11
lere tshina tsha nzimu, kwa nsonga kuti mungolimbitsidwa;
tshimene tshiri, kuti ine ndi inu dingosangalatsidwa mwa 12
inu, ife tonse ndi mvanu wa ena, inde wanu ndi wanga.
Ndimo sindifuna inu ku kala opulukira, abali, kuti ntawi 13
zambiri dinayerekeza ku fika kwa inu (ndimo dinatshedwe-
tsedwa patsogolo), kuti dinangopotshera dzobala dzina mwa
inu unso, inde monga mwa yotsala ya Mitundu. Diri wama- 14
ngawa kwa Agrike ndi kwa Abaribari, kwa anzeru ndi kwa
opusa. Tshointsho, monga didziwa, dirikuta ku uza iva- 15
ngeli ku inu unso omwe muli m' Roma. Kuti sindiri ndi 16
manyazi ndi ivangeli: kuti uli mpamvu ya Mulungu kwa
kupulumutsa kwa onse omwe amvana; kwa Myuda patso-
golo, ndi inso kwa Mgrike. Kuti momo kusonyezedwa 17
kudeka kwa Mulungu ndi mvanu kwa mvanu: monga
alembedwa, Koma wodeka adzakala ndi moyo ndi
mvanu.

Kuti kukwiira kwa Mulungu kusonyezedwa kwa kumwa- 18
mba pa kusadziwa Mulungu konse ndi kusadeka kwa antu,
omwe asindikiza nteradi m' kusadeka; tshifuka tshimene 19
tshomwe tshingodziwidwa ndi Mulungu tshisonyezedwa
mwa awo; kuti Mulungu anatshisonyeza kwa awo. Kuti 20
zintu zosaoneka za ie kwa kupanga kwa dziko zionetsedwa,
kudziwitsidwa mwa zintu zomwe zipangidwa, *inde* mpamvu
yatshi yosamariza ndi umulungu; monga kuti angokala
opanda pambanuzo: tshifuka kuti, kudziwa Mulungu, 21
sanapambanitsa ie monga Mulungu, kapena sananena
tshakoma; koma anakala autsiru mwa kukanganitsana kwao,
ndimo mitima yao yopusa inadetsedwa. Kudzisonya awo 22
oka ku kala anzeru, anakala opusa, nasintana kupambana 23
kwa Mulungu wosadziwa ku bvunda kwa kufana kwa fanizo
la muntu wobvunda, ndi la zimbalame, ndi la nyama zama-
pazi anai, ndi zokwawa.

Mwa kuti Mulungu napereka awo m' mafuno a mitima 24
yao kwa kusatsuka, kuti matupi ao akapyapyazidwa mwa
iwo oka: tshifuka kuti anasintana nteradi wa Mulu- 25
ngu kwa bodza, napembedza naimirira tshopangidwa

kopambana Mpambi, emwe ali wodala kwa magonero.
Amen.
26 Kwa tshifukwa tshimene Mulungu anapereka awo kwa
mafuno oipa: kuti akazi ao nasinta kutshita kwamakalidwe
27 kwa komwe kuli pa makalidwe: ndimo modzimodzi inso
amuna, kusia kutshita kwamakalidwe kwa nkazi, naaka m'
kufuna kwao modzi kwa wina, amuna ndi amuna kutshita
kusaoneka, ndimo kulandira mwa iwo oka kulipira kumene
kwa tshimo lao komwe kwakong'goledwa.
28 Ndimo inde monga anakana ku potshera Mulungu m'
kudziwa *kwao*, Mulungu napereka awo kwa muwongo
wotaiidwa, ku tshita zintu zidya zomwe zosali zabwino;
29 kudzazidwa ndi kusadeka konse, mpulupulu, kusirira,
kudana; odzaza ndi kudikidwa, mbanda, ndeu, tshinyengo,
30 udano; akunong'ona, amiseke, akwiiridwa ndi Mulungu,
akupepuza, onyada, odzisamalira, atintu a zintu zoipa,
31 osamvera atatu ao ndi amai ao, opanda kudziwa, akuswa
a mapangano, opanda kukonda kwamakalidwe, opanda
32 nsisi: omwe, kudziwa kumariza kwa Mulungu, kuti awo
omwe atshita zintu zotere aenera imfa, osatshita koka
zimodzimodzi, koma anso alola awo omwe atshita izo.
2 Mwa kuti uli wopanda pambanuzo, O mamuna, emwe
uli emwe uweruza: kuti m' tshomwe uweruza wina, usutsa
iwe eka; kuti iwe emwe uweruza utshita zintu zimodzi-
2 modzi. Ndimo tidziwa kuti kuweruza kwa Mulungu kuli
kofana ndi nteradi pa awo omwe ayesayesa zintu zotere.
3 Ndimo kodi uganiza tshimene, O mamuna, emwe uweruza
awo omwe ayesayesa zintu zotere, nutshita zimodzimodzi,
4 kuti udzapulumuka kuweruza kwa Mulungu? Kapena
upeputsa zolemera za ubwino watshi ndi kulekereza ndi
kumva kutali, kusadziwa kuti ubwino wa Mulungu utsogo-
5 lera iwe kwa kutembenuza ntima? koma pambuiu kuli-
mbika kwako ndi ntima wosatembenuka usunga kwa iwe
eka kukwiira m' dzua la kukwiira ndi kusonyeza kwa
6 kuweruza kodeka kwa Mulungu; emwe adzabwezera kwa
7 antu onse kofana ndi ntshito zao; ku awa omwe ndi
kulongosola m' kutshita bwino afunira kwa kupambana ndi
8 ulemu ndi kusabvunda, moyo wosamariza: koma kwa awa
omwe ali onyansidwa, ndimo osamvera nteradi, koma
9 amvera kusadeka, *zidzali* kukwiira ndi kulunduka, sautso
ndi kupwetekwa kwambiri, pa mizimu yonse ya antu yomwe
itshita mpulupulu, wa Myuda poiamba, ndi inso wa

Mgrike; koma kupambana ndi ulemu ndi ntendere kwa 10
antu onse omwe atshita ubwino, ku Myuda poiamba, ndimo
onso ku Mgrike: kuti kulibe tsang'ko ndi Mulungu. 11
Kuti monga ambiri monga anatshimwa opanda mau 12
adzamwazika anso opanda mau: ndimo monga ambiri
monga anatshimwa pansi pa mau adzaweruzidwa ndi
mau; kuti si akumva a mau ali odeka patsogolo pa Mulu- 13
ngu, koma otshita a mau adzadeketsedwa: kuti ntawi 14
Mitundu yomwe siipotshera mau itshita ndi makalidwe
zintu za mau, imene, siirikupotshera mau, iri mau kwa
iyo yoka; m' tshimene isonyeza ntshito ya mau ilembedwa 15
m' mitima yao, kudzidziwitsa kwao kumariza ndi imene, ndi
maganizo ao modzi ndi wina kutshula kapena kupambanuza
*iyo;* m' dzua lomwe Mulungu adzaweruza mabiso a antu, 16
kwa ivangeli wanga, ndi Yesu Kristu.

Koma ngati uli ndi dzina la Myuda, ndimo utsi- 17
mbirira pa mau, ndimo upambana m' Mulungu, nudziwa 18
kufuna kwatshi, nusimba zintu zomwe ziri zabwino nditu,
kupunzitsidwa kwa mau, nutshimikiza kuti iwe eka uli 19
wotsogolera wa akungu, kuunika kwa awa omwe ali
mudima, wofotokoza wa opusa, mpunzitsi wa makanda, 20
kupotshera m' mau makalidwe a kudziwa ndi a nteradi;
ndimo iwe emwe upunzitsa wina, kodi sudzipunzitsa? 21
iwe emwe uuza muntu sakanaba, kodi uba? iwe emwe 22
uti muntu sakanatshita tshigololo, kodi utshita tshigo-
lolo? iwe emwe unyansidwa ndi mafano, kodi ulanda mate-
mpile? iwe emwe upambana m' mau, mwa kuswa kwako kwa 23
mau kodi upyapyaza Mulungu? Kuti dzina la Mulungu 24
litukwanidwa mwa Mitundu tshifuka tsha inu, inde monga
alembedwa. Kuti kudula kupindula nditu, ngati ukala wotshita 25
wa mau: koma ngati ukala woswa wa mau, kudula kwako
kunakala kusadula. Ndimo ngati kusadula kusunga mamarizo 26
a mau, kodi kusadula kwatshi kusadzaganizidwa kwa kudula?
ndimo kodi kusadula komwe kuli ndi makalidwe, ngati 27
kudzaza mau, sikudzaweruza iwe, emwe ndi mlemba ndi
kudula uli woswa wa mau? Kuti ie siali Myuda, emwe 28
ali modzi kunja; kapena kumene kusali kudula, komwe
kuli kunja m' nyama: koma ie ali Myuda, emwe ali modzi 29
pakati; ndi kudula kuli kumene kwa ntima, m' nzimu, si
m' lemba; kulemekeza kwa emwe kusali kwa antu, koma
kwa Mulungu.

Ndimo kupambana kwanje apotshera Myuda? kapena 3

2 kupindula kuli kwanje kwa kudula? Kwambiri njira
zonse: patsogolo pa onse, kuti anamvanidwa ndi mau a
3 Mulungu. Kuti tshiani ngati ena anali opanda mvanu?
kodi kusauka kwao kwa mvanu kudzapanga tshabe kumva-
4 na kwa Mulungu? Si tshointsho: inde, Mulungu apeze-
dwe woona, koma antu onse onama; monga alembedwa,

Kuti unangodeketsedwa m' mau ako,
Ndimo unangopambana ntawi udza m' kuweruza.

5 Koma ngati kusadeka kwatu kubvomereza kudeka kwa
Mulungu, tidzanena tshiani? Kodi Mulungu ali wosadeka
6 emwe atsheza ndi kukwiira? (dinena kofana ndi antu). Si
tshointsho: kuti pomwe Mulungu adzaweruza dziko bwa-
7 nje? Koma ngati nteradi wa Mulungu mwa bodza langa
unatshuruka kwa kupambana kwatshi, bwanje enso kosu-
8 ntira diweruzidwa monga wampulupulu? Ndimo si
bwanje (monga tiuzidwa kodanitsa, ndimo monga ena
anenetsa tshomwe tinena), Titshite mpulupulu, kuti ubwino
ungodza? kusutsa kwa omwe kuli kodeka.

9 Ndimo tshiani? kodi tiri m' makalidwe oipa opambana
awo? Iai, palibe konse: kuti patsogolo tinandzudzula
Ayuda ndi Agrike, kuti onse ali pansi pa mpulupulu;
10 monga alembedwa,

Palibe modzi wodeka, iai, palibe modzi;
11 Palibe modzi emwe adziwitsa,
Palibe modzi emwe afuna Mulungu;
12 Onse anasotshera, akalirana osapinduka;
Palibe modzi emwe atshita bwino, iai, si inde modzi:
13 Mero wao uli mwanda wotsegula;
Ndi malilume ao anatshita tshinyengo:
Mate a ampiri ali pansi pa milomo yao:
14 Nkamwa mwa omwe mwadzaza ndi kutukwana ndi kuawa:
15 Mapazi ao ali aliwiro ku turutsa mwazi;
16 Kumwaza ndi tshisoni ziri mwa njira zao;
17 Ndi njira ya ntendere sanadziwa:
18 Kulibe kuopa kwa Mulungu patsogolo maso ao.

19 Ndimo tidziwa kuti zintu zomwe mau anena, alankula
ku awa omwe ali pansi pa mau; kuti nkamwa monse
mungoletsedwa, ndi dziko lonse lingotengedwa pansi pa
20 kuweruza kwa Mulungu: tshifuka ndi ntshito za mau
palibe nyama idzadeketsedwa m' kuona kwatshi: kuti mwa
21 mau *kudza* kudziwa kwa mpulupulu. Koma tsopano

kobaluka kwa mau kudeka kwa Mulungu kunasonyezedwa,
kumarizidwa ndi mau ndi aprofeti; inde kudeka kwa Mulu- 22
ngu mwa mvanu mwa Yesu Kristu kwa onse awo omwe
amvana; kuti kulibe kulekana; kuti onse anatshimwa, ndi 23
apereweza kupambana kwa Mulungu; kudeketsedwa kolere 24
ndi kufatsa kwatshi mwa kuombola komwe kuli mwa Kristu
Yesu: emwe Mulungu anaika patsogolo *kukala* dipo, mwa 25
mvanu, ndi mwazi watshi, kusonyeza kudeka kwatshi,
tshifuka tsha kuleka kwa zakwaipa zinatshitidwa kali, mwa
kulekereza kwa Mulungu; kwa kusonyeza, *dinena*, kwa 26
kudeka kwatshi pa nsiku yatsopano imene: kuti anango-
kala wodeka ie eka, ndi wodeketsa wa ie emwe apotshera
mvanu mwa Yesu. Ndimo kupambana kuli kuti? Kuturu- 27
tsidwa. Ndi mau anje? a zintshito? Iai: koma ndi mau
a mvanu. Ndimo tiwerenga kuti muntu adeketsedwa ndi 28
mvanu wobaluka ntshito za mau. Kapena kodi Mulungu 29
ali *Mulungu* wa Ayuda oka? kodi siali *Mulungu* wa Mitundu
unso? Inde, wa Mitundu unso: ngati kuli tshointshi kuti 30
Mulungu ali modzi, ndimo adzadeketsa kudula ndi mvanu,
ndi kusadula mwa mvanu. Ndimo kodi tipanga mau 31
atshabe mwa mvanu? Si tshointshi: iai, tilimbikitsa
mau.

Ndimo tidzanena tshiani kuti Abraham, Atatu atu 4
wakali wofana ndi nyama, wapeza? Kuti ngati Abraham 2
anadeketsedwa ndi zintshito, ali ndi mwa kuti ku pambana;
koma si kwa Mulungu. Kuti lemba linena tshiani? Ndimo 3
Abraham anamvana ndi Mulungu, ndimo kunawereng'jedwa
kwa ie kwa kudeka. Tsopano kwa ie emwe atshita, sekeretso 4
siliwereng'jedwa monga kwa kufatsa, koma monga kwa
mangawa. Koma kwa ie emwe wosatshita, koma amvana 5
ndi ie emwe adeketsa osapembedza, mvanu watshi uwere-
ng'jedwa kwa kudeka. Inde monga Davide enso atshula 6
kudala pa muntu, kwa emwe Mulungu awereng'jera kudeka
kobaluka zintshito, *kuti*, 7

> Odala ali awo mpulupulu za omwe zikulukukidwa,
> Ndimo zakwaipa za omwe zibisidwa.
> Wodala ali muntu kwa emwe Mwini wosafuna ku 8
> werenga zakwaipa.

Ndimo kodi kudala kumene kutshulidwa pa kudula, kapena 9
pa kusadula anso? kuti tinena, Kwa Abraham mvanu
watshi unawerengedwa kwa kudeka. Ndimo bwanje 10
unawerengedwa? ntawi anali m' kudula, kapena m' kusa-

11 dula? Si m' kudula, koma m' kusadula: ndimo nalandira
tshizindikilo tsha kudula, kusindikiza kwa kudeka kwa
mvanu womwe anapotshera ntawi anali m' kusadula:
kuti anangokala atate a onse omwe amvana, ngati akala
m' kusadula, kuti kudeka kunangowereng'jedwa kwa awo;
12 ndi atate a kudula kwa awo omwe si koka ali a
kudula, koma kwa omwe enso aenda m' miendo ya mvanu
umene wa atatu atu Abraham womwe anapotshera m'
13 kusadula. Kuti si mwa mau kunali kulonjezana ku Abra-
ham kapena kwa mbeu yatshi, kuti akakala woloa wa dziko,
14 koma mwa kudeka kwa mvanu. Kuti ngati awo omwe ali
a mau ali oloa, mvanu upangidwa tshabe, ndi kulonjezana
15 kupangidwa tshabe: kuti mau atshita kukwiira; koma
16 komwe kulibe mau, kapena kulibe kuswa. Kwa tshifukwa
tshimene *kuli* kwa mvanu, kuti *kungokala* kwa kufatsa;
monga kuti kulonjezana kungolimbika kwa mbeu yonse;
si kwa iyo yoka yomwe iri ya mau, koma kwa yomwe enso
17 iri ya mvanu wa Abraham, emwe ali atate a ife tonse (monga
alembedwa, Atate a mitundu yambiri dakupanga) patsogolo
pa ie emwe anamvana nai', *inde* Mulungu, emwe apanga
moyo akufa, ndimo atsha zintu zomwe siziri, monga ngati
18 zinali. Emwe m' kulingalira anamvana pa kulingalira,
monga kuti anangokala atate a mitundu yambiri, kwa
tshomwe tshinanenedwa, Tshointshi mbeu yako idzakala.
19 Ndimo kopanda kulemetsedwa mu mvanu naganiza tupi latshi
tsopano modzimodzi lofa (anali ndi dzaka pa makumi
20 okaoka kumi), ndi kufa kwa tshibaliro tsha Sara: inde,
kuyang'anira kwa kulonjezana kwa Mulungu, sanagwedera
m' kusamvana, koma analimbikitsa mu mvanu, kupatsa
21 kupambana kwa Mulungu, ndimo kubvomerezedwa nditu
kuti, tshomwe analonjezana, anali ndi mpamvu unso ku
22 tshita. Mwa kuti inso unawereng'jedwa kwa ie kwa kudeka.
23 Ndimo kusanalembedwa kwa ie eka, kuti unawereng'jedwa
24 kwa ie; koma kwa ife enso, kwa omwe udzawereng'jedwa,
omwe amvana ndi ie emwe anaukitsa Yesu Mwini watu
25 kwa akufa, emwe anaperekedwa kwa matshimo atu, ndimo
anaukitswa kwa kudeketsa kwatu.

5 Ndimo kudeketsedwa ndi mvanu, tipotshere ntendere ndi
2 Mulungu mwa Mwini watu Yesu Kristu; mwa emwe enso
tinapotshera kuyandika ndi mvanu mwa kufatsa kumene
momwe tiima; ndimo tisekere m' kulingalira kwa kupa-
3 mbana kwa Mulungu. Ndimo si tshointshi koka, koma

tisekere enso m' masautso atu: kudziwa kuti sautso itshita
kulongosola; ndi kulongosola, kuyesayesa; ndi kuyesayesa, 4
kulingalira: ndi kulingalira kusapatsa manyazi; tshifuka 5
kukonda kwa Mulungu kwawalidwa m' mitima yatu mwa
Nzimu Woyera womwe unapatsidwa kwa ife. Kuti ntawi 6
tinali kosuntira opanda mpamvu, mwa nsiku yabwino Kristu
nafera kwa osapembedza. Kuti kopereweza kwa muntu 7
wodeka modzi adzafera: kuti kapena kwa muntu wabwino
wina akayesa inde ku fera. Koma Mulungu abvomereza 8
kukonda kwatshi kwa ife, mwa kuti, ntawi tinali kosuntira
ampulupulu, Kristu nafera kwa ife. Ndimo kwambiri 9
kopambana, kudeketsedwa tsopano mwa mwazi watshi, tidza-
pulumutsidwa kwa kukwiiria *kwa Mulungu* mwa ie. Kuti 10
ngati, ntawi tinali maliwongo, tinaanjidwa kwa Mulungu
mwa imfa ya Mwana watshi, kwambiri kopambana, ku-
anjidwa, tidzapulumutsidwa mwa moyo watshi; ndimo si 11
tshointshi koka, koma anso tisekera m' Mulungu mwa Mwini
watu Yesu Kristu, mwa emwe talandira tsopano kua-
njwa.

Ndimo, monga mwa muntu modzi mpulupulu inaloa m' 12
dziko, ndi imfa mwa mpulupulu; ndi tshointsho imfa inapita
kwa antu onse, tshifuka kuti onse anatshimwa:—kuti kwa 13
ntawi ya mau mpulupulu inali m' dziko: koma mpulupulu
siiwereng'jedwa ntawi palibe mau. Koma imfa inaweruza 14
kwa Adam ku Moses, inde pa awo omwe sanatshita mpulu-
pulu pambuiu pa kufana kwa tshimo la Adam, emwe ali
sonyezo la ie emwe analikufika. Koma si monga tshimo, 15
tshointshi inso *tshiri* tshaulere tshaufulu. Kuti ngati ndi
tshimo la modzi ambiri nafa, kwambiri kopambana kufatsa
kwa Mulungu, ndi tshaulere mwa kufatsa kwa muntu modzi,
Yesu Kristu, zinatshuruka kwa ambiri. Ndimo si monga 16
mwa modzi emwe natshimwa, *tshointshi* tshiri tshaulere:
kuti kuweruza *kunadza* ndi modzi kwa kusautsa, koma
tshaulere tshaufulu *tshinafika* ndi matshimo ambiri kwa ku-
deketsa. Kuti ngati, ndi tshimo la modzi, imfa inaweruza 17
mwa modzi; kwambiri kopambana omwe alandira kutshu-
ruka kwa kufatsa ndi kwa tshaulere tsha kudeka adzaweruza
m' moyo mwa modzi, *inde* Yesu Kristu. Ndimo tshointsho 18
monga mwa tshimo limodzi *kuweruza kunafika* kwa antu onse
kwa kusautsa; inde tshointsho mwa ntshito imodzi ya
kudeka *tshaulere tshaufulu tshinadza* kwa antu onse kwa
kudeketsa kwa moyo. Kuti monga mwa kusamvera kwa 19

muntu modzi ambiri anapangidwa ampulupulu, inde tshoi-
ntsho mwa kumvera kwa modzi ambiri adzadeketsedwa.
20 Ndimo mau anso analoa, kuti tshimo linangotshuruka;
koma pomwe mpulupulu inatshuruka, kufatsa kunatshuruka
21 kwambiri kopambana: kuti, monga mpulupulu inaweruza
mwa imfa, inde tshointsho kufatsa kunangoweruza mwa
kudeka kwa moyo wosamariza mwa Yesu Kristu Mwini
watu.

6 Ndimo tidzanena tshiani? Kodi tidzakalabe m' mpulu-
2 pulu, kuti kufatsa kutshuruke? Si tshointsho. Ife tomwe
tinafa kwa mpulupulu, bwanje tidzakala ntawi inso momo?
3 Kapena kodi muli opulukira kuti ife tonse tomwe tinabapa-
tizidwa mwa Kristu Yesu tinabapatizidwa mwa imfa yatshi?
4 Ndimo tinaikidwa m' mwanda ndi ie mwa mbapatisma mwa
imfa: kuti kofana monga Kristu anaukitswa kwa akufa
mwa kupambana kwa Atate, tshointshi ife enso tinangoenda
5 m' utsopano wa moyo. Kuti ngati takala omangidwa ndi
*ie* m' kufana kwa imfa yatshi, tidzakala anso *ndi kufana* kwa
6 kuukirira kwatshi.; kudziwa tshimene, kuti umuntu watu
wakali unapatshikidwa ndi *ie*, kuti tupi la mpulupulu lina-
ngotshotsedwa, kuti tshointsho sitikakala ntawi ina m'
7 umpawi kwa mpulupulu; kuti iemwe wafa adeketsedwa
8 kwa mpulupulu. Koma ngati tinafa ndi Kristu, timvana
9 kuti tidzakala m' moyo onso ndi ie; kudziwa kuti Kristu
anaukitswa kwa akufa wosafa ntawi ina; imfa yosaweruza
10 ntawi ina pa ie. Kuti imfa yomwe anafa, anafa tshimodzi
kwa mpulupulu: koma moyo womwe akala ndi moyo,
11 akala ndi moyo kwa Mulungu. Inde tshointsho werengani
inu noka anso akufa kwa mpulupulu, koma amoyo kwa
Mulungu mwa Kristu Yesu.
12 Ndimo musaleka mpulupulu ku weruza m' tupi lanu lakufa,
13 kuti mukamvera mafuno a ilo: kapena musapatsa dziwalo
dzanu kwa mpulupulu *monga* dzipangizo dza kusadeka;
koma patsani inu noka kwa Mulungu, monga amoyo kwa
akufa, ndi dziwalo dzanu *monga* dzipangizo dza kudeka kwa
14 Mulungu. Kuti mpulupulu yosadzaweruza pa inu: kuti
musali pansi pa mau, koma pansi pa kufatsa.
15 Ndimo bwanje? kodi tidzatshimwa, tshifuka sitiri pansi
16 pa mau, koma pansi pa kufatsa? Si tshointsho. Kodi
musadziwa, kuti kwa emwe mupatsa inu noka *monga* akapolo
kwa kumvera, akapolo atshi muli emwe mumvera; kapena
a mpulupulu kwa imfa, kapena a kumvera kwa kudeka?

Koma tshakoma kwa Mulungu, kuti, mwa kuti munali 17
akapolo a mpulupulu, munakala omvera kwa ntima kwa
sonyezo lidya la kupunzitsa kwa Iomwe munaperekedwa;
ndimo kunapatsidwa ufulu kwa mpulupulu, munakala 18
akapolo a kudeka. Dinena kofana ndi antu tshifuka tsha 19
kufoka kwa nyama yanu: kuti monga munapatsa dziwalo
dzanu *monga* akapolo kwa kusatsuka ndi kwa mpulupulu
kwa mpulupulu, inde tshointsho tsopano mupatsa dziwalo
dzanu *monga* akapolo kwa kudeka kwa kuyeretsa. Kuti 20
ntawi munali akapolo a mpulupulu, munali aufulu ndi
kudeka. Ndimo tshobala tshanje munapotshera pa ntawi 21
idya m' zintu mwa zomwe tsopano muli ndi manyazi? kuti
nsonga ya zintu zimenezo iri imfa. Koma tsopano kunapa- 22
ngidwa ufulu kwa mpulupulu, ndimo munakala akapolo kwa
Mulungu, mupotshera tshobala tshanu kwa kuyeretsa, ndi
nsonga moyo wosamariza. Kuti kulipira kwa mpulupulu 23
kuli imfa; koma tshaulere tshaufulu tsha Mulungu tshiri
moyo wosamariza m' Kristu Yesu Mwini watu.

Kapena muli opulukira, abali (kuti dilankula ndi antu 7
omwe adziwa mau), bwanje kuti mau aweruza muntu kwa
ntawi yonse yomwe ali ndi moyo? Kuti nkazi emwe ali 2
ndi mamuna amangidwa ndi mau kwa mamuna ntawi ali
ndi moyo; koma ngati mamuna afa, amasulidwa kwa mau
a mamuna. Ndimo tshointshi ngati, ntawi mamuna ali ndi 3
moyo, amangidwa kwa muntu wina, adzatshedwa nkazi wa
tshigololo: koma ngati mamuna afa, amasuka kwa mau,
monga kuti wosali nkazi wa tshigololo, ngati amangidwa
kwa muntu wina. Mwa kuti, abali anga, inu unso muna- 4
pangidwa akufa kwa mau mwa tupi la Kristu; kuti
mukamangidwa kwa wina, *inde* kwa ie emwe anaukitswa kwa
akufa, kuti tinangobala tshobala kwa Mulungu. Kuti 5
ntawi tinali m' nyama, mafuno a zoipa, omwe anali mwa
mau, anatshita m' dziwalo dzatu ku bala tshobala kwa imfa.
Koma tsopano tamasulidwa kwa mau, kunafa kwa tshomwe 6
mwa kuti tinagwidwa; monga kuti tiimirira m' utsopano
mwa nzimu, ndimo si m' ukali wa mlemba.

Ndimo tidzanena tshiani? Kodi mau ali mpulupulu? 7
Si tshointsho. Koma, sindinadziwa mpulupulu, kani mwa
mau: kuti sindinadziwa kusinjirira, kani mau ananena,
Usasinjirira: koma mpulupulu, kupeza tshifukwa, inatshita 8
mwa ine mwa mau mitundu yonse ya kusinjirira: kuti
kobaluka mau mpulupulu *iri* yakufa. Ndimo dinali ndi 9

moyo kobaluka mau *ntawi* imodzi : koma ntawi mau nafika,
10 mpulupulu inatsitsimuka, ndinafa ; ndi mau, omwe *anali*
11 kwa moyo, amene dinapeza *kuli* kwa imfa : kuti mpulupulu,
kupeza tshifukwa, mwa mau inanyenga ine, ndi mwa awo
12 inapa ine. Monga kuti mau ali oyera, ndi mau oyera, ndi
13 odeka, ndi abwino. Ndimo kodi omwe ali abwino anakala
imfa kwa ine? Si tshointsho. Koma mpulupulu, kuti
inangosonyezedwa iri mpulupulu, ndi kutshita imfa kwa ine
mwa tshomwe tshiri tshabwino ;—kuti mwa mau mpulupulu
14 inangokala mpulupulu yopambana. Kuti tidziwa kuti mau
ali anzimu : koma diri wanyama, dinagulitsidwa pansi
15 pa mpulupulu. Kuti tshomwe ditshita sindidziwa : kuti si
tshomwe difuna, tshomwe ditshita ; koma tshomwe dikwiira,
16 tshomwe ditshita. Koma ngati tshomwe sindifuna, tshomwe
17 ditshita, dibvomera ku mau kuti ali abwino. Ndimo tsopano
sitshiri inso ine emwe ditshitshita, koma mpulupulu yomwe
18 ikala mwa ine. Kuti didziwa kuti mwa ine, tshomwe
tshiri, m' nyama yanga, tshikala palibe kantu kabwino : kuti
kufuna kuli ndi ine, koma ku tshita tshomwe tshiri
19 tshabwino si*kuli*. Kuti ubwino womwe difuna sinditshita :
koma tshoipa tshomwe sindifuna, tshomwe ditshita.
20 Koma ngati tshomwe sindifuna, tshomwe ditshita,
sitshiri ntawi ina ine emwe ditshitshita, koma mpulupulu
21 yomwe ikala mwa ine. Ndimo dipeza mau, kuti, kwa ine
22 emwe difuna ku tshita abwino, tshoipa tshiripo. Kuti
disekera m' mau a Mulungu pambuiu muntu ali mkati :
23 koma diona mau ena m' dziwalo dzanga, kumenyana ndi
mau a muwongo wanga, ndi kutenga ine mwa ukapolo
pansi pa mau a mpulupulu omwe ali m' dziwalo dzanga.
24 O muntu wosauka emwe diri! ndani adzapulumutsa ine
25 mwa tupi la imfa imene? Dinena tshakoma kwa Mulungu
mwa Yesu Kristu Mwini watu. Ndimo tshointshi ine
ndeka ndi muwongo diimirira mau a Mulungu ; koma ndi
nyama mau a mpulupulu.

8 Ndimo tsopano kulibe kusutsa kwa awa omwe ali m
2 Kristu Yesu. Kuti mau a Nzimu wa moyo m' Kristu Yesu
3 anamasula ine kwa mau a mpulupulu ndi a imfa. Kuti
tshomwe mau osadziwa ku tshita, mwa kuti anali ofoka
mwa nyama, Mulungu, kutumiza Mwana watshi m' kufana
kwa nyama ya mpulupulu ndimo *monga nsembe* kwa
4 mpulupulu, nasutsa mpulupulu m' nyama : kuti kufuna
kwa mau kunangodzazidwa mwa ife, omwe osaenda

pambuiu nyama, koma pambuiu nzimu. Kuti awo omwe 5
ali pambuiu nyama asamala zintu za nyama; koma awo
omwe ali pambuiu nzimu zintu za nzimu. Kuti muwongo 6
wa nyama uli imfa; koma muwongo wa nzimu uli moyo ndi
ntendere: tshifuka muwongo wa nyama uli kukwia pa 7
Mulungu; kuti usali pansi pa mau a Mulungu, kapena
nditu sudziwa ku kala: ndimo awo omwe ali m' nyama 8
osadziwa ku sekeretsa Mulungu. Koma simuli m' 9
nyama, koma m' nzimu, ngati nditu Nzimu wa Mulungu
ukala mwa inu. Koma ngati muntu modzi wosapotshera
Nzimu wa Kristu, siali modzi wa ie. Ndimo ngati Kristu 10
ali mwa inu, tupi liri lakufa tshifuka tsha mpulupulu;
koma nzimu uli moyo tshifuka tsha kudeka. Koma 11
ngati Nzimu wa iemwe anaukitsa Yesu kwa akufa ukala
mwa inu, iemwe anaukitsa Kristu Yesu kwa akufa adzafulu-
miza anso matupi anu akufa mwa Nzimu watshi womwe
ukala mwa inu.

Ndimo tshointsho, abali, tiri amangawa, si kwa nyama, ku 12
kala ndi moyo pambuiu pa nyama: kuti ngati mukala ndi 13
moyo pambuiu pa nyama, mukanafa; koma ngati ndi
nzimu mufetsa ntshito za tupi, mudzakala ndi moyo. Kuti 14
monga ambiri monga atsogozwa ndi Nzimu wa Mulungu,
amene ali ana a Mulungu. Kuti simunapotshera nzimu wa 15
umpawi inso kwa kuopa; koma munalandira nzimu wa
kusunga, ndi womwe tipfulira, Aba, Atate. Nzimu iwo 16
woka umariza ndi mizimu yatu, kuti tiri ana a Mulungu:
ndimo ngati ana, pomwe oloa; oloa a Mulungu, ndimo 17
oloaanzatshi ndi Kristu; ngati nditu timva ndi *ie*, kuti inso
tingopambanitsidwa ndi *ie*.

Kuti diwerenga kuti kumva kwa ntawi imene yatsopano 18
sikuli koenera ku linganizidwa ndi kupambana komwe
kudzasonyezedwa kwa ife. Kuti kulingalira kolimba kwa 19
kupanga kulinda kwa kusonyeza kwa ana a Mulungu.
Kuti kupanga kunaikidwa pansi pa utsiru, si kwa kufuna 20
kwatshi, koma ndi tshifukwa tsha ie emwe nakuika pansi,
m' kulingalira kuti kupanga koka anso kudzapulumutsidwa 21
kwa umpawi wa kubvunda m' ufulu wa kupambana kwa
ana a Mulungu. Kuti tidziwa kuti kupanga konse kubulira 22
ndi kumva ululu pa modzi kwa tsopano. Ndimo si 23
tshointsho koka, koma ife toka anso, omwe apotshera
dzobala dzoiamba dza Nzimu, inde ife toka tibulira mwa ife
toka, kulindira kusunga *kwatu*, *inde*, kuombola kwa tupi

24 latu. Kuti ndi kulingalira tinapulumutsidwa: koma
kulingalira komwe kuonedwa sikuli kulingalira: kuti
25 ndani alingalira tshomwe aona? Koma ngati tilingalira
tshomwe sitiona, *pomwe* ndi kulongosola tilindira itsho.
26 Ndimo modzimodzi Nzimu unso utangata kufoka kwatu:
kuti sitidziwa bwanje ku pempera monga tikana*pempera;*
koma Nzimu woka upembedzera kwa *ife* ndi mabuliro omwe
27 sakanatshulidwa; ndimo iemwe asaka mitima adziwa
tshomwe tshiri muwongo wa Nzimu, tshifuka apembedzera
28 kwa oyera kofana ndi *kufuna kwa* Mulungu. Ndimo
tidziwa kuti kwa awo omwe akonda Mulungu zintu zonse
zitshita pa modzi kwa ubwino, *inde* kwa awo omwe
29 aitanidwa kofana ndi kuyerekeza *kwatshi.* Kuti omwe
anadziwa patsogolo, nalimbitsa kali inso ku fanikizidwa kwa
kufaniza kwa Mwana watshi, kuti anangokala woiamba ku
30 badwa mwa abali ambiri: ndimo omwe nalimbitsa kali, awo
onso anaitana: ndimo omwe anaitana, awo onso anadeketsa,
ndimo omwe anadeketsa, awo onso anapambanitsa.
31 Ndimo tidzanena tshiani ndi zintu zimenezi? Ngati
32 Mulungu *ali* kwa ife, ndani *ali* pa ife? Iemwe sanaianja
Mwana watshi, koma napereka ie kwa ife tonse, bwanje
33 enso ndi ie sadzapatsa ife kolere zintu zonse? Ndani
adzatshula kantu pa osang'ka a Mulungu? Ali Mulungu
34 emwe adeketsa; ndani ali ie emwe adzasutsa? Ali Kristu
Yesu emwe anafa, inde kopambana, emwe anaukitswa kwa
akufa, emwe akala pa dzanja lamanja la Mulungu, emwe
35 enso apembedzera kwa ife. Ndani adzagawa ife kwa kukonda
kwa Kristu? kodi sautso, kapena kupweteka kwambiri,
kapena nkarwe, kapena njala, kapena marisetshe, kapena
36 kutsekerezwa, kapena mpeni wa nkondo? Inde monga
alembedwa,

Kwa iwe tipedwa siku lonse;
Tinawerengedwa monga nkosa kwa kupa.

37 Iai, mwa zintu zonse zimenezi tiri kopambana ndi opambana
38 mwa emwe anakonda ife. Kuti dikantshiziridwa, kuti
kapena imfa, kapena moyo, kapena anjelo, kapena maufumu,
kapena zintu zatsopano, kapena zintu zidza, kapena
39 zimpamvu, kapena kuzuka, kapena kuya, kapena kupanga
kwina, sizidzakala ndi mpamvu ku gawa ife kwa kukonda
kwa Mulungu, komwe kuli m' Kristu Yesu Mwini watu.

9 Dinena nteradi m' Kristu, sindinama, kudzidziwitsa
2 kwanga kuweruza ndi ine m' Nzimu Woyera, kuti diri ndi

tshisoni tshambiri ndi ululu wosaleka m' ntima wanga.
Kuti didziwa ku funa kuti ine ndeka diri wotukwanidwa 3
kwa Kristu kwa abali anga, abali anga pambuiu pa nyama:
omwe ali Asirayeli; kwa omwe ziri kusunga, ndi kupa- 4
mbana, ndi mapangano, ndi kupatsa kwa mau, ndi kuimirira
*kwa Mulungu*, ndi malonjezano; a omwe ali atate, ndi wa 5
omwe ali Kristu, monga ndi nyama, emwe ali wopambana
onse, Mulungu wodala kwa magonero. Amen. Koma *si* 6
*kuli* monga ngati mau a Mulungu anafika kwa tshabe.
Kuti osali onse Sirayeli, omwe ali a Sirayeli: kapena, 7
tshifuka ali mbeu ya Abraham, siali onse ana: koma, m'
Yisake mbeu yako idzaitanidwa. Tshomwe tshiri, si ali 8
ana a nyama omwe ali ana a Mulungu; koma ana a
kulonjezana awerengedwa kwa mbeu. Kuti amene ali mau 9
a kulonjezana, kwa ntawi imene didzafika, ndimo Sara
adzakala ndi mwana. Ndimo si tshointsho koka; koma 10
Rebeka anso anabvuuka ndi modzi, *inde* ndi atatu atu
Yisake—kuti *ana* tsopano sanabadwa, kapena sanatshita 11
kantu kwabwino kapena koipa, kuti kuyerekeza kwa
Mulungu pambuiu pa kusang'ka kunangoima, si kwa
zintshito, koma kwa ie emwe aitana, anenedwa ndi ie, 12
Wang'kuru adzaimirira wang'ono. Inde monga alembedwa, 13
Yakobi dakonda, koma Esau dinakwiira.

Ndimo tidzanena tshiani? Kodi kuli kusadeka ndi 14
Mulungu? Si tshointsho. Kuti anena ndi Moses, 15
Didzakala ndi nsisi pa omwe dikala ndi nsisi, ndimo
didzakala ndi tshisoni pa omwe dikala ndi tshisoni. Ndimo 16
tshointsho si kuli kwa ie emwe afuna, kapena kwa ie emwe
atamanga, koma kwa Mulungu emwe akala ndi nsisi. Kuti 17
lemba linena kwa Faro, Kwa kuyerekeza kumene nditu
dinaukitsa iwe, kuti dinangosonyeza mwa iwe mpamvu
yanga, ndimo kuti dzina langa linangokumbutsidwa m'
dziko lonse. Ndimo tshointsho akala ndi nsisi pa omwe 18
afuna, ndi omwe afuna alimbikitsa.

Ndimo udzanena ndi ine, bwanje asuliza kosuntira? Kuti 19
ndani aima pa kufuna kwatshi? Iai koma, O muntu, uli 20
ani emwe uiang'ka pa Mulungu? Kodi tshintu tshopa-
ngidwa tshidzanena kwa ie emwe anatshipanga, Bwanje
unandipanga ine tshointsho? Kodi kapena wakuomba 21
mbia siakala ndi kwatshi pa dote, kwa buma limodzi ku
omba pande limodzi tshiwira kwa ulemu, ndi tshina kwa
kusalemekeza? Ndimo ngati Mulungu, kufuna ku sonya 22

kukwiira kwatshi, ndi ku dziwitsa mpamvu yatshi,
anamvabe ndi kumva kwakutali dziwira dza kukwiira
23 dzikonzedwa kwa kumwazika: ndimo kuti anangodziwitsa
zolemera za kupambana kwatshi pa dziwira dza nsisi,
24 dzomwe anafotokoza kali kwa kupambana, *inde* ife, tomwe
enso anaitana, si kwa Ayuda oka, koma anso kwa Mitundu?
25 Monga anena anso m' Hosheya,

Didzatsha omwe antu anga, omwe sanali antu ánga;
Ndi ie wokondedwa, emwe sanali wokondedwa.
26 Ndimo tshidzakala, *kuti* m' malo pomwe tshinanenedwa
ndi awo, Si muli antu anga,
Apo adzatshedwa ana a Mulungu wamoyo.

27 Ndimo Yesaya apfula ndi Sirayeli, Ngati kuwerenga kwa
ana a Sirayeli kukala monga ntshenga wa nyanja, kuli kutsala
28 komwe kudzapulumutsidwa: kuti Mwini adzatshita mau
29 *atshi* pa dziko, kuata ndi kuadula pafupi. Ndimo, monga
Yesaya wanena kali,

Kani Mwini wa Magulu anatisia mbeu,
Tinakala monga Sodom, ndimo tinapangidwa kofana
ndi Gomora.

30 Ndimo tidzanena tshiani? Kuti Mitundu, yomwe isanatsata
pambuiu kudeka, inafika kwa kudeka, inde kudeka komwe
31 kuli ndi mvanu: koma Sirayeli, kutsata mau a kudeka,
32 sanafika kwa mau *amene*. Bwanje? Tshifuka *sanaafuna* ndi
mvanu, koma monga tshinali ndi zintshito. Anapuntwa pa
33 mwala wa kupuntwa; inde monga alembedwa,

Ona, diika m' Ziyon mwala wa kupuntwa ndi tantwe
la kwiitsa:
Ndimo iemwe amvana ndi ie sadzapatsidwa manyazi.

10 Abali, kufuna kwa ntima wanga ndi pempo langa ku
2 Mulungu ziri kwa awo, kuti angopulumutsidwa. Kuti
dimariza awo kuti apotshera utshitsanzo kwa Mulungu,
3 koma si kwa kudziwa. Kuti kusadziwa ndi kudeka kwa
Mulungu, ndi kufuna ku limbitsa kwao, sanaika awo oka
4 pansi pa kudeka kwa Mulungu. Kuti Kristu ali nsonga ya
5 mau kwa kudeka kwa onse omwe amvana. Kuti Moses
alemba kuti muntu emwe atshita kudeka komwe kuli kwa
6 mau adzakala ndi moyo ndi iko. Koma kudeka komwe
kuli ndi mvanu kunena tshointshi, Usanena muntima wako,
Ndani adzakwera m' mwamba? (tshomwe tshiri, ku tsitsa
7 Kristu:) kapena, Ndani adzatsika m' kuya? (tshomwe
8 tshiri, ku kweza Kristu kwa akufa.) Koma kunena

tshiani? Mau ali pafupi ndi iwe, m' nkamwa mwako, ndi
muntima mwako: omwe ali, mau a mvanu, omwe tiuza:
tshifuka ngati udzabvomera ndi nkamwa mwako Yesu 9
*monga* Mwini, ndimo udzamvana muntima mwako kuti
Mulungu anaukitsa ie kwa akufa, udzapulumutsidwa: kuti 10
ndi ntima muntu amvana kwa kudeka; ndimo ndi nkamwa
kubvomera kupangidwa kwa kupulumutsa. Kuti lemba 11
liti, Emwe amvana ndi ie sadzapatsidwa manyazi. Kuti 12
kulibe kusiana pakati pa Myuda ndi Mgrike: kuti *Mwini*
modzimodzi ali Mwini wa onse, ndimo ali wolemera kwa
onse omwe aitana pa ie: kuti, Emwe adzaitana pa dzina la 13
Mwini adzapulumutsidwa. Ndimo bwanje adzaitana pa ie 14
mwa emwe sanamvana? ndimo bwanje adzamvana mwa ie
ndi emwe sanamva? ndimo bwanje adzamva opanda wouza?
ndimo bwanje adzauza, kani atumidwa? inde monga 15
alembedwa, Bwanje abwino ali mapazi a awo omwe atenga
makalidwe osekera a zintu zabwino!

Koma sanamva onse ndi ivangeli. Kuti Yesaya ati, 16
Mwini, ndani wamvana mbiri yatu? Tshointsho mvanu 17
*udza* ndi kumva, ndi kumva ndi mau a Kristu. Koma 18
dinena, kodi sanamva? Inde, nditu,

Namalowe wao naturuka m' dziko lonse,
Ndi mau ao kwa zinsonga za dziko.

Koma dinena, Kodi Sirayeli sanadziwa? Poiamba 19
Moses ati,

Didzadwetsa ku nsanje inu ndi womwe wosali mtundu,
Ndi mtundu wopanda kudziwitsa didzakwiitsa inu.

Ndimo Yesaya ali wolimbika ntima nditu, ndimo ati, 20

Dinapezedwa ndi omwe sanafuna ine;
Dinasonyezedwa kwa omwe sanafunsa ndi ine.

Koma monga ndi Sirayeli ati, Siku lonse dinayala manja 21
anga kwa antu osamvera ndi anseke.

Ndimo dinena, Kodi Mulungu anataia antu atshi? Si 11
tshointsho. Kuti ine enso diri Msirayeli, wa mbeu ya
Abraham, wa fuko la Benyamin. Mulungu sanataia antu 2
atshi omwe nadziwa patsogolo. Kapena kodi musanadziwa
tshiani lemba liti mwa Eliya? bwanje apempa ndi Mulungu
pa Sirayeli, Mwini, anapa aprofeti ako, anagumula akatshisi 3
ako: ndimo disiidwa ndeka, ndimo afuna moyo wanga.
Koma bvomero la Mulungu linena tshiani ndi ie? Dasia 4
kwa ine ndeka antu mazousan asanu ndi awiri, omwe
sanagwada bondo kwa Bali. Ndimo inde tshointshi pa 5

ntawi imene yatsopano onso alipo otsala kwa kusang'ka
6 kwa kufatsa. Koma ngati kuli ndi kufatsa, sikuli inso
7 kwa zintshito: kani kufatsa si kuli inso kufatsa. Ndimo
tshiani? Tshomwe Sirayeli afunira, tshimene sanalandira:
koma kusang'ka kunalandira itsho: ndimo otsala anali-
8 mbikitsidwa: monga alembedwa, Mulungu napatsa awo
nzimu woledzedwa, maso kuti sakaona, ndi makutu kuti
9 sakamva, kwa siku limene nditu. Ndimo Davide anena,
Gome lao lipangidwe nsampa, ndi mbuna,
Ndi lopuntwa, ndi kulipira kwa awo:
10 Maso ao angodetsedwe, kuti sangoona,
Ndimo ukotetsa mbuiu yao ntawi zonse.
11 Ndimo dinena, Kodi napuntwa kuti anangogwa? Si
tshointsho: koma ndi kugwa kwao kupulumutsa *kunadza*
12 kwa Mitundu, ku dwetsa awo ku nsanje. Ndimo ngati
kugwa kwao kuli zolemera za dziko, ndi kumwazamwaza kwao
zolemera za Mitundu; bwanje opambana kutshuruka kwao?
13 Koma dinena ndi inu omwe muli Mitundu. Ndimo
tshointshi monga diri mpostile wa Mitundu, dipambanitsa
14 kuimirira kwanga: ngati ndi kantu dingodwetsa ku nsanje
*awo omwe ali* nyama yanga, ndimo dingopulumutsa ena a
15 awo. Kuti ngati kutaia kwa awo *kuli* kuanjana kwa dziko,
tshiani *kudzali* kulandira *kwa awo*, koma moyo kwa akufa?
16 Ndimo ngati tshobala tshoiamba tshiri tshoyera, tshointshi
tshiri buma: ndimo ngati ntsitsi uli woyera, tshointshi ziri
17 ntambi. Koma ngati zina za ntambi zinatsholedwa, ndimo
iwe, kuli olive lamtengo, unakomanizidwa mwa awo, ndimo
unakala wogawa ndi awo kwa ntsitsi wa zolemera za ntengo
18 wa olive; usapambana pa zintambi: koma ngati upambana,
19 siuli iwe emwe ubala ntsitsi, koma ntsitsi iwe. Pomwe
udzanena, Ntambi zinatsholedwa, kuti dinangokomanizidwa.
20 Nanga; ndi kusamvana kwao zinatsholedwa, ndimo iwe
uima ndi mvanu wako. Sudzakala wodzitama, koma opa:
21 kuti ngati Mulungu sanaianja ntambi za makalidwe, kapena
22 sadzaianja iwe. Ndimo ona ubwino ndi kulimba za
Mulungu: kwa awo omwe anagwa, kulimba; koma kwa
iwe, ubwino wa Mulungu, ngati ukalabe m' ubwino
23 watshi: kani udzadulidwa anso. Ndimo awo onso, ngati
osakalabe m' kusamvana kwao, adzakomanitsidwa: kuti
24 Mulungu ali ndi mpamvu ku komaniza awo onso. Kuti
ngati unadulidwa kwa womwe uli ndi makalidwe ntengo
wa olive lamtengo, ndimo unakomanizidwa pa makalidwe

muntengo wa olive wabwino: bwanje kopambana zimene,
zomwe ziri *ntambi* zamakalidwe, zidzakomanizidwa muntengo
wa olive wao?

Kuti sindifuna inu ku kala opulukira, abali, ndi kusadzi- 25
wika kumene, kani muli otshenjera m' maganizo anu, kuti
kulimbika m' pande kunafika kwa Sirayeli, kwa kudzaza
kwa Mitundu kunaloa; ndimo tshointsho Sirayeli onse 26
adzapulumutsidwa: inde monga alembedwa,

Womasula adzaturuka m' Ziyon;
Adzatembenuza kusapembedza kwa Yakobi:
Ndimo kumene kuli kupangana kwanga kwa awo, 27
Ntawi didzatshotsa zakwaipa zao.

Monga ndi ivangeli, ali maliwongo kwa inu: koma 28
monga ndi kusang'ka, ali okondedwa kwa atate. Kuti 29
zolere ndi kuitana za Mulungu ziri zopanda kutembenuza
ntima. Kuti monga inu m' ntawi yapita munali osamvera 30
kwa Mulungu, koma tsopano munalandira nsisi ndi kusa-
mvera kwao, inde tshointsho tsopano amene enso anakala 31
osamvera, kuti ndi nsisi inasonyedwa kwa inu awo onso
tsopano angolandira nsisi. Kuti Mulungu watsekera onse 32
kwa kusamvera, kuti anangokala ndi nsisi kwa onse.

O kuya kwa zolomera ndi nzeru ndi kudziwa za Mulungu! 33
bwanje kusasaka ali maweruzo atshi, ndi njira zatshi
zopambana ku tsata! Kuti ndani wadziwa muwongo wa 34
Mwini? kapena ndani wakala nkoswe watshi? kapena 35
ndani poiamba wapatsa kwa ie, ndimo tshidzalipidwa kwa
ie enso? Kuti ndi ie, ndi mwa ie, ndi kwa ie, ziri zintu 36
zonse. Kwa ie *kukale* kupambana kwa magonero. Amen.

Ndimo, abali, dipempa inu ndi nsisi za Mulungu, ku 12
patsa matupi anu nsembe yamoyo, yoyera, yoseketsa kwa
Mulungu, *komwe kuli* kuimirira kotshenjera kwanu.
Ndimo musaombedwa kwa kugonera kumene: koma 2
musandutsidwa ndi kupanga kwatsopano kwa muwongo
wanu, kuti mungoyesa komwe kuli kufuna kwabwino ndi
koseketsa ndi kwakuta kwa Mulungu.

Kuti dinena, mwa kufatsa komwe kunapatsidwa ine, kwa 3
antu onse omwe ali mwa inu, si ku ganiza ndi awo oka
kopambana ndi komwe akanaganiza; koma tshointshi ku
ganiza monga ku ganiza kodziweruza, kofana ndi Mulungu
wapatsa ku antu onse muyezo wa mvanu. Kuti inde 4
monga tiri ndi dziwalo dzambiri m' tupi limodzi, ndimo
dziwalo dzonse dzosali ndi udindo umodzi: tshointsho ife, 5

tomwe tiri ambiri, tiri tupi limodzi m' Kristu, ndi onse dziwalo
6 modzi wa wina. Ndimo tiri ndi zaulere kulekana kofana
ndi kufatsa komwe kunapatsidwa kwa ife, ngati kulosa,
7 *tilose* kwa kuyezera kwa mvanu watu; kapena kuimirira,
tidzipatse kwa kuimirira kwatu; kapena iemwe apunzitsa,
8 kwa kupunzitsa kwatshi; kapena iemwe alungamitsa, kwa
kulungamitsa kwatshi: iemwe apatsa, adzatshite ndi ntima
umodzi; iemwe aweruza, ndi tshangu; iemwe asonyeza nsisi,
9 ndi kusekera. Kukonda kukale kopanda tshinyengo. Kwi-
irani ndi tshomwe tshiri tshoipa; gwirizani ndi tshomwe
10 tshiri tshabwino. M' kukonda kwa abali kondanani bwino;
11 m' ulemu kuika modzi ndi wina patsogolo; m' tshangu si
kutshedwa; kutentedwa munzimu; kuimirira Mwini;
12 kusekera m' kulingalira; kulongosola m' sautso; kukalabe
13 kolimbika m' kupempera; kupatsa kwa mafunidwo a
14 oyera; kutsata kuyang'anira aulendo. Dalitsani awo omwe
15 azunza inu; dalitsani, ndi musatukwana. Sekerani ndi
16 omwe asekera; lirani nsozi ndi omwe alira nsozi. Kalani
ndi ntima umodzi, modzi ndi wina. Musaika mitima
yanu pa zintu zazikuru, koma mudzitshepetse kwa zintu
zomwe ziri zofatsa. Musatshenjera m' maganizo anu.
Musabweza mpulupulu kwa mpulupulu kwa muntu modzi.
17 Yang'anirani kwa zintu zaulemu m' kuona kwa antu onse.
Ngati mudziwa, monga ambiri monga kuli mwa inu,
18 kalani ndi ntendere ndi antu onse. Musazimbula inu noka,
19 okondedwa, koma patsa malo kwa kukwiira: kuti alembe-
dwa, Kuzimbula kuli kwanga; didzalipira, ati Mwini.
Koma ngati liwongo lako limva njala, eta ilo; ngati limva
20 ludzu, patsa ilo ku mwa: kuti ndi kutshita tshointshi
udzaunjika makala a moto pa mutu patshi. Usapambani-
21 dwa ndi mpulupulu, koma pambana mpulupulu ndi ubwino.
Mizimu yonse ikale pansi pa mpamvu zopambana: kuti
13 kulibe mpamvu koma kwa Mulungu; ndi *mpamvu* zomwe
zikala ziloezedwa ndi Mulungu. Ndimo ie emwe akana
2 mpamvu, akana kuloeza kwa Mulungu: ndi awo omwe
akana adzalandira kwa awo oka kuweruza. Kuti oweruza
3 osali kuopetsa kwa ntshito yabwino, koma kwa yoipa.
Ndimo ufuna ku kala kopanda kuopa kwa mpamvu? tshita
tshomwe tshiri tshabwino, ndimo udzalandira kulemekeza
kwa yomwe: kuti iri woimirira wa Mulungu kwa iwe kwa
4 ubwino. Koma ngati utshita tshomwe tshiri mpulupulu,
opa; kuti isanyamula mpeni wa nkondo kwa tshabe: kuti iri

woimirira wa Mulungu, wozimbula kwa kukwiira kwa iemwe
atshita mpulupulu. Mwa kuti mukanakala pansi, si koka 5
tshifuka tsha kukwiira, koma anso kwa kudzidziwitsa. Kuti 6
kwa tshifukwa tshimene mulipira tsong'ko onso; kuti ziri
oimirira a kuimirira kwa Mulungu, kuimirira ntawi yonse pa
tshintu tshimenetshi nditu. Patsani ku onse gong'gole zao: 7
tsong'ko kwa emwe tsong'ko *lingokong'goledwa;* lipiro kwa
emwe lipiro; kuopa kwa emwe kuopa; ulemu kwa emwe
ulemu.

Musakong'gola kantu kwa muntu modzi, koma ku 8
kondana: kuti ie emwe akonda woiandikila watshi wadzaza
mau. Kuti tshimene, Usatshita tshigololo, Usapa, Usaba, 9
Usasinjirira, ndimo ngati alipo mau ena, aong'khetsedwa m'
mau amene, tshointshi, Udzakonda woiandikila wako monga
iwe eka. Kukonda kutshita palibe mpulupulu kwa woia- 10
ndikila watshi: ndimo kukonda kuli kudzaza kwa mau.

Ndimo tshimene, kudziwa nsiku, kuti tsopano iri ntawi 11
yeitali kwa inu ku uka kwa tulo: kuti tsopano kupulumutsa
kuli pafupi kwa ife kopambana ntawi *tinaamba* ku mvana.
Utali wa usiku unapita, ndimo msana uli pafupi: ndimo 12
titaie ntshito za ndima, ndimo tibvale ntshinjirizo wa
kuunika. Tiende bwino, monga m' dzua; si m' kudzedze- 13
duka ndi kuledzera, si m' tshigololo ndi kuyaluka, si m'
ndeu ndi nsanje. Koma bvalani Mwini Yesu Kristu, ndimo 14
musakwanira kwa nyama, ku *dzaza* mafuno *a iyo.*

Koma ie emwe ali wopanda mpamvu m' mvanu landirani, 14
*kosuntira* si kwa makangano oganizaganiza. Muntu modzi 2
ali ndi mvanu ku dia zintu zonse: koma iemwe ali wopanda
mpamvu adia zitsamba. Iemwe adia siapute iemwe wosadia; 3
ndimo iemwe wosadia siaweruze iemwe adia: kuti Mulungu
walandira ie. Uli ani emwe aweruza bandazi wa wina? 4
Ku mwini watshi aima kapena agwa. Inde, adzaimitsidwa;
kuti Mwini ali ndi mpamvu ku imitsa ie. Muntu modzi 5
aweruza dzua limodzi kopambana lina: wina aweruza
masiku onse *modzimodzi.* Antu onse alimbitsidwe m'
mauongo ao. Iemwe aganiza ndi siku, aganiza ndi ilo 6
kwa Mwini: ndi iemwe adia, adia kwa Mwini, kuti anena
tshakoma kwa Mulungu; ndimo iemwe wosadia, kwa Mwini
wosadia, ndimo wosanena tshakoma kwa Mulungu. Kuti 7
palibe modzi wa ife akala ndi moyo kwa ie eka, ndimo
palibe modzi afa kwa ie eka. Kuti ngati tikala ndi moyo, 8
tikala ndi moyo kwa Mwini; kapena ngati tifa, tifa kwa

Mwini: ndimo ngati tikala ndi moyo, kapena tifa, tiri a
9 Mwini. Kuti kwa nsonga imene Kristu anafa, ndimo nakala
ndi moyo *onso*, kuti anangokala Mwini wa akufa ndi wa
10 amoyo. Koma iwe, bwanje uweruza mbali wako? kapena
iwe enso, bwanje uputa mbali wako? kuti ife tonse tidzaima
11 patsogolo pa mpando wa kuweruza wa Mulungu. Kuti
alembedwa,

Monga dikala ndi moyo, ati Mwini, kwa ine maondo
onse adzagwada,
Ndi malilume onse adzabvomera kwa Mulungu.

12 Ndimo tshointsho ife tonse tidzawereng'jera ndi ife toka kwa
Mulungu.
13 Ndimo lekani ife si ku weruzana anso: koma weruzani
tshimene kopambana, kuti palibe muntu aika tshopuntwa m'
14 njira ya mbali watshi, kapena tshokwiitsa. Didziwa, ndimo
dikantshiziridwa m' Mwini Yesu, kuti palibe kantu kali
kosatsuka m' iko koka: kani kuti ku iemwe aganiza kantu
15 kosatsukidwa, kwa ie kali kosatsuka. Kuti ngati tshifuka
tsha kudia mbali wako amvetsedwa tshisoni, usapita anso m'
kukonda. Usamwaza ndi kudia kwako ie kwa emwe Kristu
16 nafera. Ndimo musaleka ubwino wanu ku nenedwa zoipa
17 nawo: kuti dziko la Mulungu siliri kudia ndi kumwa, koma
kudeka ndi ntendere ndi tshimwemwe m' Nzimu Woyera.
18 Kuti ie emwe m' tshimene aimirira Kristu ali wosekera ndi
19 Mulungu, ndi wasimbidwa ndi antu. Ndimo tshointshi
titsate pambuiu pa zintu zomwe zipanga kwa ntendere, ndi
20 zintu ndi zomwe tingomangirana. Musatembenuza kwa
kudia ntshito ya Mulungu. Zintu zonse nditu zira zotsuka;
koma tshiri tshoipa kwa muntu amene emwe adia ndi
21 tshimo. Tshiri tshabwino si ku dia nyama, kapena si ku
mwa vinyo, kapena si *ku tshita kantu* komwe kapuntwitsa
22 mbali wako. Mvanu womwe upotshera, potshera kwa iwe
eka patsogolo Mulungu. Wosekera ali ie emwe wosaweruza
23 ie eka m' tshimene tshomwe asimba. Koma ie emwe agani-
zaganiza asutsidwa ngati adia, tshifuka *adia* si ndi mvanu;
ndi tshomwe tshosali tsha mvanu tshiri mpulupulu.

15 Ndimo ife tomwe tiri olimba tikananyamula mafoko a
omwe opanda mpamvu, ndimo si ku sekeretsa ife toka.
2 Leka ife tonse ku sekeretsa woiandikila watu kwa tshimene
3 tshomwe tshiri tshabwino, kwa kumangira. Kuti Kristu unso
sanasekeretsa ie eka; koma, monga alembedwa, Dzidzumo
4 dza omwe anadzuma iwe dzinagwa pa ine. Kuti zintu

zomwe zinalembedwa kali zinalembedwa kwa kupunzira
kwatu, kuti mwa kulongosola ndi mwa kusangalatsa za
malemba tinangopotshera kulingalira. Ndimo Mulungu 5
wa kulongosola ndi wa kusangalatsa apatse inu ku kala ndi
muwongo umodzi modzi ndi wina kwa Kristu Yesu: kuti 6
ndi ntima umodzi ndi nkamwa modzi mungopambanitsa
Mulungu ndi Atate a Mwini watu Yesu Kristu. Ndimo 7
landiranani, inde monga Kristu unso analandira inu, kwa
kupambana kwa Mulungu. Kuti dinena kuti Kristu wapa- 8
ngidwa woimirira wa kudula kwa nteradi wa Mulungu, kuti
anangolimbikitsa malonjezano *anapatsidwa* kwa atate, ndimo
kuti Mitundu inangopambanitsa Mulungu kwa nsisi yatshi; 9
monga alembedwa,

Ndimo didzalemekeza iwe mwa Mitundu,
Ndidzaimba kwa dzina lako.

Ndimo onso ati, 10

Sekerani, Mitundu inu, ndi antu atshi.

Ndimo onso, 11

Lemekezani Mwini, inu nonse Mitundu;
Ndimo antu onse alemekeze ie.

Ndimo onso, Yesaya ati, 12

Udzali ntsitsi wa Yishayi,
Ndi iemwe auka ku weruza pa Mitundu;
Pa ie Mitundu idzalingalira.

Ndimo Mulungu wa kulingalira adzaze inu ndi tshimwemwe 13
tshonse ndi ntendere m' kumvana, kuti mungotshuruka m'
kulingalira, m' mpamvu ya Nzimu Woyera.

Ndi ine ndeka anso dikantshirizidwa ndi inu, abali anga, 14
kuti inu noka muli odzaza ndi ubwino, odzaza ndi kudziwa
konse, muli ndi mpamvu unso ku ambirirana. Koma 15
dilemba kolimbika kopambana kwa inu ndi pande, monga
kukumbutsa inu unso, tshifuka tsha kufatsa komwe
kunapatsidwa kwa ine ndi Mulungu, kuti dikakala woimi- 16
rira wa Kristu Yesu kwa Mitundu, kuimirira ivangeli wa
Mulungu, kuti kutira kwa Mitundu kunangopangidwa
kosekera, kuyeretsedwa ndi Nzimu Woyera. Ndimo 17
dipotshera kupambana kwanga m' Kristu Yesu m' zintu
za Mulungu. Kuti sindidzayesa ku lankula ndi zintu 18
zina kani ndi zimenezo zomwe Kristu natshita mwa
ine, kwa kumvera kwa Mitundu, ndi mau ndi ntshito, m' 19
mpamvu ya zizindikilo ndi zozizwa, m' mpamvu ya Nzimu
Woyera; monga kuti kwa Yerusalem, ndi lozungulira inde

20 kwa Liriko, dinauza kodzaza ivangeli wa Kristu; inde, kuku-
panga kutanda kwanga tshointsho ku uza ivangeli, si pomwe
Kristu anatshedwa *kali*, kuti sindinangomanga pa kuzika kwa
21 muntu wina; koma, monga alembedwa,

Adzaona, kwa omwe palibe makalidwe a ie anafika,
Ndi awo omwe sanamva adzadziwitsa.

22 Mwa kuti inso dinatshedwetsedwa ntawi zambiri zimenezi
23 kwa kudza kwa inu: koma tsopano, kusapotshera palibe malo
ena m' maiko amene, ndimo kupotshera dzaka dzambiri dzi-
24 mene kufuna kudza kwa inu, ntawi yomwe dimuka kwa
Spaniya (kuti dilingalira ku ona inu m' ulendo wanga, ndi
ku tengedwa pa njira yanga yauko ndi inu, ngati poiamba,
25 ndi pande, dikanadzakwaniridwa ndi unzanu)—koma tsopano,
26 *diti*, ding'ka ku Yerusalem, kuimirira kwa oyera. Kuti
kunali kusekera kwabwino kwa Makedoniya ndi Akaya
kupanga kupatsa kumene kwa osauka mwa oyera omwe ali
27 pa Yerusalem. Inde, kunali kusekera kwabwino kwao;
ndimo amangawa ao ali. Kuti ngati Mitundu inapangidwa
ogawa a zintu zanzimu zao, akong'gola *ku awa* anso ku
28 imirira ku awo m' zintu zanyama. Ndimo ntawi data
tshimene, ndimo dasindikiza ku awo tshobala tshimene,
29 didzapita ndi inu kwa Spaniya. Ndimo didziwa kuti,
ntawi difika kwa inu, didzafika m' kudzaza kwa kudala kwa
Kristu.

30 Ndimo dipempa inu, abali, ndi Mwini watu Yesu Kristu,
ndimo ndi kukonda kwa Nzimu, kuti muyesana pa modzi
31 ndi ine m' mapempero anu ku Mulungu kwa ine; kuti dingo-
pulumutsidwa kwa awo omwe ali osamvera m' Yudeya, ndi
*kuti* kuimirira kwanga komwe *diri nako* kwa Yerusalem
32 kungokala kosekera kwa oyera; kuti dingofika kwa inu m'
tshimwemwe m' kufuna kwa Mulungu, ndimo ndi inu
33 dingopeza kupuma. Ndimo Mulungu wa ntendere akale
ndi inu nonse. Amen.

16 Dibvomereza kwa inu Foyibe mlongwatu, emwe ali
2 woimirira wa eklesia lomwe liri pa Kenkreya: kuti
mulandira ie m' Mwini, koenera kwa oyera, ndi kuti
mutangata ie m' tshintu tshomwe angofunidwa ndi inu:
kuti ie eka anso wakala wotangata wa ambiri, ndi wa ine
ndeka.

3 Utsani Priska ndi Akwila otshita anzanga m' Kristu Yesu,
4 omwe kwa moyo wanga naika pansi makosi ao; kwa omwe
si oka dipatsa tshakoma, koma anso maeklesia onse a

Mitundu: ndimo *utsani* eklesia lomwe liri m' nyumba yao. 5
Utsani Paineto wokondedwa wanga, emwe ali dzobala-dzoi-
amba dza Asiya kwa Kristu. Utsani Mariya, emwe 6
napatsa ntshito zambiri pa inu. Utsani Androniko ndi 7
Yuniyas, anzanga, ndi omangidwa abali anga, omwe ali a
mbiri mwa apostile, omwe enso anakala m' Kristu patsogolo
pa ine. Utsani Ampliyato wokondedwa wanga m' Mwini. 8
Utsani Urbano wotshita nzatu m' Kristu, ndi Stakis 9
wokondedwa wanga. Utsani Apeles wobvomeredwa m' 10
Kristu. Utsani awo omwe ali a *banja* la Aristobulo. Utsani 11
Herodiyon mbali wanga. Utsani awo a *banja* la Narkiso,
omwe ali m' Mwini. Utsani Trifaina ndi Trifosa, omwe 12
atshita m' Mwini. Utsani Perses wokondedwa, emwe
natshita kwambiri m' Mwini. Utsani Rufo wosang'kidwa 13
m' Mwini, ndi amai wa ie ndi wa ine. Utsani Asinkrito, 14
Filegon, Hermes, Patrobas, Hermas, ndi abali omwe ali nao.
Utsani Filologo ndi Yuliya, Nereyis ndi mlongwatshi, ndi 15
Limpas, ndi oyera onse omwe ali nao. Utsanani ndi 16
kumsomsona koyera. Maeklesia onse a Kristu autsa
inu.

Ndimo dipempa inu, abali, yang'anirani awo omwé apanga 17
magano ndi zifukwa za kwiitsa, pa kupunzitsa komwe
munapunzira: ndimo tembenukani kwa awo. Kuti omwe 18
ali otere osaimirira Mwini watu Kristu, koma mimba zao;
ndimo ndi kunena kwao kosalala ndi kubvomereza anyenga
mitima ya osatshimwa. Kuti kumvera kwanu kunakula ku 19
antu onse. Ndimo disekera pa inu: koma difuna inu ku
kala otshenjera kwa tshomwe tshiri tshabwino, ndi osanyenga
kwa zintu zomwe ziri zoipa. Ndimo Mulungu wa ntendere 20
adzapondereza Satana pansi pa mapazi anu mwa ntawi
yeing'ono.

Kufatsa kwa Mwini watu Yesu Kristu kukale ndi inu.

Timote wotshita nzanga autsa inu; ndi Lukiyo ndi Yason 21
ndi Sosipatro, abali anga. Ine Tertiyo, emwe dilemba 22
epistola, diutsa iwe m' Mwini. Gayo mwini-wa-nyumba 23
wanga, ndi wa eklesia lonse, autsa inu. Erasto wosunga
zolemera wa mzinda autsa inu, ndi Kwarto mbali.

Ndimo kwa ie emwe ali ndi mpamvu ku limbikitsa inu 25
kwa ivangeli wanga ndi kuuza kwa Yesu Kristu, kwa
kusonyeza kwa kusadziwika komwe kwasungidwa m'
kutontola mwa ntawi zosamariza, koma tsopano kusonyeze- 26
dwa, ndi mwa malemba a aprofeti, kwa mau a Mulungu

wosamariza, kudziwitsidwa kwa mitundu yonse kwa kumvera
27 kwa mvanu; kwa Mulungu wotshenjera eka, mwa Yesu
Kristu, kwa emwe kuli kupambana kwa magonero. Amen.

---

## EPISTOLA LATSHIMODZI LA PAULOS KWA

# AKORINTE.

1 PAULOS, aitanidwa *ku kala* mpostile wa Yesu Kristu
mwa kufuna kwa Mulungu, ndi Sostene mbali watu,
2 kwa eklesia la Mulungu lomwe liri pa Korinte, *inde* awo
omwe ayeretsedwa m' Kristu Yesu, aitanidwa *ku kala* oyera,
ndi onse omwe aitana pa dzina la Mwini watu Yesu Kristu
3 m' malo onse, *Mwini* wao ndi watu: Kufatsa kwa inu ndi
ntendere kwa Mulungu Atatu atu ndi Mwini Yesu Kristu.
4 Dinena tshakoma kwa Mulungu wanga ntawi yonse ndi
inu, kwa kufatsa kwa Mulungu komwe kunapatsidwa kwa
5 inu m' Kristu Yesu; kuti m' zintu zonse munalemezedwa
6 mwa ie, m' mau onse ndi kudziwa konse; inde monga
7 kumariza kwa Kristu kunalimbitsidwa mwa inu: monga
kuti musapereweza m' tshaulere tshonse; kulinda kwa
8 kusonyeza kwa Mwini watu Yesu Kristu; emwe enso adza-
limbitsa inu kwa nsonga, *monga kuti mudzakala* osasulumu-
9 lidwa m' siku la Mwini watu Yesu Kristu. Mulungu ali
wamvanu, mwa emwe munaitanidwa m' unzatshi wa Mwana
watshi Yesu Kristu Mwini watu.
10 Tsopano dipempa inu, abali, mwa dzina la Mwini watu
Yesu Kristu, kuti munena nonse tshintu tshimodzi, ndimo
*kuti* kukale palibe magawo mwa inu; koma *kuti* mudzate-
tsedwa pa modzi m' muwongo umodzi ndi m' kuweruza
11 kumodzi. Kuti kunasonyezedwa kwa ine ndi inu, abali
anga, ndi awo *omwe ali a banja* la Klowe, kuti ali makangano
12 mwa inu. Koma tshimene dinena, kuti inu nonse munena,
Diri wa Paulos; ndi ine wa Apolo; ndi ine wa Kefa; ndi
13 ine wa Kristu. Kodi Kristu agawidwa? Kodi Paulos
anapatshikidwa kwa inu? kapena munabapatizidwa m'

dzina la Paulos? Dinena tshakoma kwa Mulungu kuti 14
sindinabapatiza modzi wa inu, koma Krispo ndi Gayo; kani 15
muntu modzi akanena kuti munabapatizidwa m' dzina langa.
Ndimo dinababapatiza anso banja la Stefana: kopambana, 16
sindidziwa ngati dinababapatiza modzi wina. Kuti Kristu 17
sanatumiza ine ku bapatiza, koma ku uza ivangeli: si m'
nzeru ya mau, kani nkhwitshi ya Kristu ikapangidwa
tshabe.

Kuti mau a nkhwitshi ali ku awo omwe alikumwazika 18
kupusa; koma kwa ife tomwe tirikupulumutsidwa ali
mpamvu ya Mulungu. Kuti alembedwa, 19

Didzamwaza nzeru za anzeru,
Ndimo tshisao tsha atshisao didzakana.

Wanzeru ali kuti? wolembera ali kuti? wakukangana 20
wa kugonera kumene ali kuti? kodi Mulungu sanapusitsa
nzeru za dziko? Kuti kuona kuti m' nzeru ya Mulungu 21
dziko mwa nzeru yatshi lisanadziwa Mulungu, kunali
kusekera kwabwino kwa Mulungu mwa kupusa kwa
kuuza ku pulumutsa awo omwe amvana. Kuona kuti 22
Ayuda afunsa kwa zizindikilo, ndi Agrike afunira nzeru:
koma tiuza Kristu apatshikidwa, kwa Ayuda kukwii- 23
tsa, ndi kwa Mitundu kupusa; koma kwa omwe aitani- 24
dwa, Ayuda ndi Agrike, Kristu mpamvu ya Mulungu, ndi
nzeru za Mulungu. Tshifuka kupusa kwa Mulungu kuli 25
kwanzeru kopambana antu; ndi kufoka kwa Mulungu kuli
kolimba kopambana antu.

Kuti onani kuitana kwanu, abali, bwanje kuti si ambiri 26
anzeru pambuiu pa nyama, si ambiri ampamvu, si ambiri
otshuka, *aitanidwa:* koma Mulungu nasang'ka zintu zopusa 27
za dziko, kuti anangopatsa manyazi kwa awo omwe ali anzeru;
ndimo Mulungu nasang'ka zintu zofoka za dziko, kuti ana-
ngopatsa manyazi kwa zintu zomwe ziri zolimba; ndi zintu 28
zatshabe za dziko, ndi zintu zomwe zinyozedwa, Mulungu
anasang'ka, *inde* ndi zintu zomwe zosali, kuti anangopepu-
tsa zintu zomwe ziri: kuti palibe nyama ikapambana patso- 29
golo pa Mulungu. Koma wa ie muli m' Kristu Yesu, emwe 30
anapangidwa kwa ife nzeru kwa Mulungu, ndi kudeka ndi
kuyeretsa, ndi kuombola: kuti, ndi monga alembedwa, 31
Emwe apambana, apambane m' Mwini.

Ndimo ine, abali, ntawi dinafika kwa inu, dinafika si ndi 2
ubwino wa mau kapena wa nzeru, kuuza kwa inu kusadzi-
wika kwa Mulungu. Kuti dinayerekeza si kudziwa kantu 2

3 mwa inu, koma Yesu Kristu, ndi ie wapatshikidwa. Ndimo
dinali ndi inu m' kufoka, ndi m' kuopa, ndi m' kuntuntumira
4 kwambiri. Ndimo mau anga ndi kuuza kwanga sizinali ndi
mau okantshizira a nzeru, koma m' kusonyeza kwa Nzimu
5 ndi kwa mpamvu: kuti mvanu wanu usakaima mwa nzeru
za antu, koma m' mpamvu ya Mulungu.
6 Koma tilankula nzeru mwa akuta: kosuntira nzeru si za
kugonera kumene, kapena si za oweruza a kugonera kumene,
7 omwe adzatopeputsa: koma tilankula nzeru za Mulungu m'
kusadziwika, zomwe zabisidwa, zomwe Mulungu anaika kali
8 patsogolo pa magonero kwa kupambana kwatu: zomwe
palibe modzi wa oweruza a kugonera kumene adziwa: kuti
ngati anazidziwa, sakanapatshika Mwini wa kupambana:
9 koma monga alembedwa,

Zintu zomwe diso silinaona, ndi kutu silinamva,
Ndi *zomwe* zisanaloa m' ntima wa muntu,
Zintu zomwe Mulungu anafotokoza kwa awo omwe akonda ie.

10 Koma kwa ife Mulungu anasonyeza *izo* mwa Nzimu: kuti
Nzimu ufuna zintu zonse, inde, zintu zakuya za Mulungu.
11 Kuti ndani mwa antu adziwa zintu za muntu, koma nzimu
wa muntu, womwe uli mwa ie? inde tshointsho zintu za
Mulungu palibe modzi adziwa, koma Nzimu wa Mulungu.
12 Koma tinalandira, si nzimu wa dziko, koma nzimu womwe
uli wa Mulungu; kuti tinangodziwa zintu zomwe zipatsidwa
13 kolere kwa ife ndi Mulungu. Zintu zomwe enso tilankula,
si m' mau omwe nzeru za muntu zipunzitsa, koma omwe
Nzimu upunzitsa; kufanizira zintu zanzimu ndi zanzimu.
14 Koma muntu wamakalidwe wosalandira zintu za Nzimu wa
Mulungu: kuti ziri kupusa kwa ie; ndimo wosadziwa ku
15 dziwa izo, tshifuka kuti ziweruzidwa kwanzimu. Koma ie
emwe ali wanzimu aweruza zintu zonse, ndi ie eka wosa-
16 weruzidwa ndi muntu modzi. Kuti ndani wadziwa muwongo
wa Mwini, kuti akapunzitsa ie? Koma tiri ndi muwongo
wa Kristu.

3 Ndimo ine, abali, sindinadziwa ku lankula ndi inu monga
kwa anzimu, koma monga kwa anyama, monga kwa tiana
2 tamanja m' Kristu. Dinalera inu ndi nkaka, si ndi nyama;
tshifuka simunali kosuntira ndi mpamvu *kuitenga:* iai, inde
3 tsopano simudziwa; kuti muli kosuntira anyama: kuti
monga kutiziripo mwa inu nsanje ndi ndeu, kodi simuli
4 anyama, ndi mupita pambuiu makalidwe a antu? Kuti

ntawi modzi anena, Diri wa Paulos; ndi wina, Diri wa
Apolo; kodi simuli antu? Ndimo Apolo ali ani? ndi 5
Paulos ali ani? Oimirira mwa omwe munamvana; ndi
onse monga Mwini napatsa ku awo. Dinaoka, Apolo natsi- 6
rira; koma Mulungu napatsa kukulitswa. Ndimo tshoi- 7
ntsho kapena ie emwe aoka wosali kantu, kapena ie emwe
atsirira; koma Mulungu emwe akulitsa. Ndimo ie emwe 8
aoka ndi ie emwe atsirira ali modzi: koma onse adzalandira
sekeretso lao kwa ntshito yao. Kuti tiri otshita anzatshi 9
ndi Mulungu: muli ulimi wa Mulungu, kumanga kwa
Mulungu.

Kwa kufatsa kwa Mulungu komwe kunapatsidwa kwa 10
ine, monga womanga-mbuiye wanzeru dinaika kuzika;
ndimo wina amanga pa iko. Koma onse ayang'anire bwanje
amanga pa iko. Kuti kuzika kwina palibe muntu adziwa ku 11
ika koma kumene komwe kuikidwa, komwe kuli Yesu
Kristu. Koma ngati muntu modzi amanga pa kuzika golide, 12
silivere, miala yolemera, ntengo, he, dziputu; ntshito ya 13
onse idzasonyezedwa: kuti siku lidzaiuza, tshifuka isonye-
zedwa m' moto; ndi moto woka udzayesa ntshito ya onse ndi
mtundu wanje iri. Ngati ntshito ya muntu modzi idzaka- 14
labe yomwe inamanga ipo, adzalandira sekeretso. Ngati 15
ntshito ya muntu modzi idzaotshedwa, adzamva kutaia:
koma ie eka adzapulumutsidwa; koma tshointsho monga
mwa moto.

Kodi simudziwa kuti muli malo oyera a Mulungu, 16
ndi *kuti* Nzimu wa Mulungu ukala mwa inu? Ngati 17
muntu modzi amwaza malo oyera a Mulungu, ie Mulungu
adzamwaza; kuti malo oyera a Mulungu ali oyera,
omwe muli.

Palibe muntu modzi adzinyenge. Ngati muntu modzi 18
aganiza kuti ali wanzeru mwa inu m' kugonera kumene,
akale wopusa, kuti angokala wanzeru. Kuti nzeru za dziko 19
limene ziri kupusa ndi Mulungu. Kuti alembedwa, Iemwe
atenga anzeru m' kutshenjera kwao: ndimo onso, Mwini 20
adziwa masing'ko a anzeru, kuti ali tshabe. Mwa kuti 21
palibe modzi apambane mwa antu. Kuti zintu zonse ziri 22
zanu; kapena Paulos, kapena Apolo, kapena Kefa, kapena
dziko, kapena moyo, kapena imfa, kapena zintu zatsopano,
kapena zintu zirinkudza; zonse ziri zanu; ndimo muli a 23
Kristu; ndi Kristu ali wa Mulungu.

Tshointshi muntu awerenge ndi ife, monga ndi oimirira 4

2 a Kristu, ndi adindo a kusadziwika za Mulungu. Pano,
kopambana, kufunidwa m' adindo, kuti muntu apezedwa
3 wamvanu. Koma ndi ine tshiri tshintu tshatshing'ono
nditu kuti dikaweruzidwa ndi inu, kapena ndi kuweruza
4 kwa muntu: inde, sindiweruza ine ndeka. Kuti didziwa
palibe kantu pa ine ndeka; koma sindideketsedwa ndi
5 kumene: koma ie emwe aweruza ine ali Mwini. Mwa kuti
musaweruza kantu patsogolo pa ntawi, kwa ntawi Mwini
afika, emwe adzasonya zintu zobisidwa za ndima, ndimo
adzasonyeza maweruzo a mitima; ndimo pomwe antu onse
adzapotshera kulemekeza kwao kwa Mulungu.
6 Koma zintu zimenezi, abali, m' sonyezo dinatshotsa ndi-
naika pa ine ndi pa Apolo kwa inu; kuti mwa ife munango-
punzira si *ku pita* kunja kwa zintu zomwe zilembedwa; kuti
7 palibe modzi wa inu atupitsidwa kwa modzi pa wina. Kuti
ndani apanga iwe ku siana? ndimo upotshera tshiani
tshomwe usanalandira? koma ngati unatshilandira, bwanje
8 upambana, monga ngati usanatshilandira? Kali munadza-
zidwa, kali munalemera, munaweruza opanda ife: inde
ndimo ndifuna kuti muweruze, kuti ife enso tingoweruza
9 ndi inu. Kuti, diganiza, Mulungu anaika ife apostile
pambuiu pa onse, monga antu asutsidwa kwa imfa: kuti
tipangidwa kuona kwa dziko, ndi kwa anjelo, ndi kwa antu.
10 Tiri opusa kwa Kristu, koma muli otshenjera mwa Kristu;
tiri ofoka, koma muli olimba; muli ndi kupambana, koma
11 ife tiri ndi kusalemekeza. Inde kwa ora latsopano timva
njala, ndi ludzu, ndimo tiri omariseke, ndimo titunduzidwa,
12 ndimo tiri alendo; ndimo titshita kwambiri, kutshita ndi
13 manja atu: kutukwanidwa, tidalitsa; kuzunzidwa, timvabe;
kunamiziridwa, tipempa: tipangidwa monga zotaia za dziko,
dzinyalala dza zintu zonse, inde kwa tsopano.
14 Sindilemba zintu zimenezi ku patsa manyazi kwa inu,
15 koma ku taulira inu monga ana anga okondedwa. Kuti
ngati mukali ndi ampunzitsi mazousan kumi m' Kristu,
kosuntira *musali ndi* atate ambiri: kuti m' Kristu Yesu
16 dinabala inu mwa ivangeli. Ndimo dipempa inu, kalani
17 ofanizira a ine. Kwa tshifukwa tshimene datumiza kwa
inu Timote, emwe ali mwana wanga wokondedwa ndi
wamvanu m' Mwini, emwe adzakumbutsa inu ndi njira
zanga zomwe ziri m' Kristu, inde monga dipunzitsa m' malo
18 onse m' maeklesia onse. Ndimo ena atupitsidwa, monga
19 ngati sindirikufika kwa inu. Koma didzafika kwa inu

nsanga, ngati Mwini afuna ; ndimo didzadziwa, si mau a omwe
atupitsidwa, koma mpamvu. Kuti dziko la Mulungu siliri 20
m' mau, koma m' mpamvu. Mufuna tshiani? kodi didza- 21
fika kwa inu ndi ntole, kapena m' kukonda ndi nzimu wa
kuanja?

Kunabukitsidwa nditu kuti liripo dama mwa inu, ndi 5
dama lotere monga losali inde mwa Mitundu, kuti modzi *wa*
*inu* wapotshera nkazi wa atatu atshi. Ndimo mutupitsidwa, 2
ndimo musanafuna kopambana ku kala ndi nsoni, kuti ie
emwe anatshita ntshito imene anangotshotsedwa mwa inu.
Kuti ine nditu, diri kutali ndi tupi koma pano ndi nzimu, 3
monga ngati dinali apo, kali daweruza ie emwe tshointsho
anatshita tshintu tshimene, m' dzina la Mwini watu Yesu, 4
munasong'kanidwa, ndi nzimu wanga, ndi mpamvu ya Mwini
watu Yesu, ku pereka modzi wotere kwa Satana kwa 5
kumwaza kwa nyama, kuti nzimu ungopulumutsidwa m'
dzua la Mwini Yesu. Kupambana kwanu si kuli kwabwino. 6
Kodi musadziwa kuti fumba yeing'ono itupa buma lonse?
Tsukitsani fumba yakali, kuti mungokala buma latsopano, 7
inde monga simutupitsidwa. Kuti mpasika watu unso
watsiridwa, *inde* Kristu: mwa kuti tisunge kudia, si ndi 8
fumba yakali, kapena ndi fumba ya madano ndi ya mpulu-
pulu, koma ndi nkate wopanga tshabe wa kuona ndi wa
nteradi.

Dinalemba kwa inu m' epistola langa si ku dzipatika ndi 9
adama; si konse ndi adama a dziko lino, kapena ndi osinji- 10
rira ndi oawanya, kapena ndi opembedza mafano; kuti
pomwe mukanaturuka kwa dziko: koma tsopano dilemba 11
kwa inu si ku dzipatika, ngati muntu modzi emwe atshedwa
mbali akala wadama, kapena wosinjirira, kapena wopembedza
mafano, kapena wonyoza, kapena woledzera, kapena woawa-
nya; ndi modzi tshointsho iai, si ku dia. Kuti dirikutshita 12
tshiani ndi kuweruza awo omwe ali kunja? Kodi simuwe-
ruza awo omwe ali momo, koma omwe ali kunja Mulungu 13
aweruza? Tshotsani muntu woipa kwa mwa inu noka.

Kodi alipo modzi wa inu, ali ndi mrandu pa woiandikila 6
watshi, ayesa ku enda ndi mrandu patsogolo pa osadeka, ndi
si patsogolo pa oyera? Kapena simudziwa kuti oyera 2
adzaweruza dziko? ndimo ngati dziko liweruzidwa ndi inu,
kodi muli osaenera ku weruza zintu zazing'ono zopambana?
Kodi simudziwa kuti tidzaweruza anjelo? bwanje kopa- 3
mbana, zintu zomwe ziri za moyo umene? Ndimo ngati 4

mukanaweruza ndi zintu zomwe ziri za moyo umene, kodi
5 muika awo ku weruza omwe ali atshabe m' eklesia? Dinena
*tshimene* ku patsa inu manyazi. Kodi tshiri tshointshi, kuti
kusadziwa *ku pezedwa* mwa inu muntu modzi wanzeru, emwe
6 adzadziwa ku lekanitsa mwa abali atshi, koma mbali aenda
7 ndi mrandu ndi mbali, ndi kumene patsogolo osamvana? Iai,
kali liri konse tshimo mwa inu, kuti muli ndi mirandu modzi
ndi wina. Bwanje kopambana musalandira tshimo? bwanje
8 kopambana musatshenjereredwa? Iai, koma inu noka mu-
9 tshimwa, ndi mutshenjerera, ndi tshimene abali *anu*. Kape-
na simudziwa kuti osadeka sadzaloa m' dziko la Mulungu?
Musanyengedwa: kapena si adama, kapena si opembedza
mafano, kapena si atshigololo, kapena si alesi, kapena si
10 akuyaruka, kapena si ambala, kapena si osinjirira, kapena si
oledzera, kapena si onyoza, kapena si oawanga, adzaloa m'
11 dziko la Mulungu. Ndimo otere anali ena a inu: koma
munasambitsidwa, koma munayeretsedwa, koma munadeke-
tsedwa m' dzina la Mwini Yesu Kristu, ndi m' Nzimu wa
Mulungu watu.
12 Zintu zonse ziri zamau kwa ine; koma si zintu zonse ziri
zopindulira. Zintu zonse ziri zamau kwa ine; koma sindi-
13 funa ku tengedwa pansi pa mpamvu ya tshimodzi. Zakudia
kwa mimba, ndi mimba kwa zakudia: koma Mulungu adza-
tenga kwa tshabe iyo ndi izo. Koma tupi losali kwa dama,
14 koma kwa Mwini; ndi Mwini kwa tupi: ndimo Mulungu
inde anaukitsa Mwini, ndimo adzaukitsa ife mwa mpamvu
15 yatshi. Kodi simudziwa kuti matupi anu ali dziwalo dza
Kristu? Kodi pomwe didzatshotsa dziwalo dza Kristu,
napanga idzo dziwalo dza nkazi-wadama? Si tshointsho.
16 Kapena simudziwa kuti iemwe adzipatikidwa ndi nkazi-
wadama ali tupi limodzi? kuti, Awa awiri, ati, adzakala
17 nyama imodzi. Koma ie emwe adzipatikidwa ndi Mwini ali
18 nzimu umodzi. Tawani dama. Mpulupulu zonse zomwe
muntu atshita ziri kunja kwa tupi; koma ie emwe atshita
19 dama atshita mpulupulu pa tupi latshi loka. Kapena simu-
dziwa kuti tupi lanu liri malo oyera a Nzimu Woyera
womwe uli mwa inu, womwe mupotshera kwa Mulungu?
20 ndimo simuli wanu; kuti munagulidwa ndi ntengo: ndimo
pambanitsani Mulungu m' tupi lanu.
7 Koma ndi zintu ndi zomwe munalemba: Tshiri tshabwino
2 kwa muntu si ku tosa nkazi. Koma, tshifuka tsha madama,
antu onse apotshere akazi ao oka, ndi akazi onse apotshere

amuna ao oka. Mamuna apatse kwa nkazi gong'gole yatshi: 3
ndimo tshointshi inso nkazi kwa mamuna. Nkazi wosali ndi 4
mpamvu pa tupi latshi, koma mamuna: ndimo tshointshi
inso mamuna wosali ndi mpamvu pa tupi latshi, koma nkazi.
Musatshenjererana, kani kuli ndi kulolana kwa nsiku, kuti 5
mungodzipatsa kwa kupempera, ndimo mungoli pa modzi
inso, kuti Satana wosanyenga inu tshifuka tsha kusadzinga
kwanu. Koma tshimene dinena ndi kulola, si ndi mau. 6
Koma difuna kuti antu onse anali inde monga ine 7
ndeka. Koma antu onse ali ndi zaulere zao kwa Mulungu,
modzi pambuiu makalidwe amene, ndi wina pambuiu
adya.

Koma dinena ndi osakwata ndi akazi amasie, Tshiri 8
tshabwino kwa awo ngati akalabe inde monga ine. Koma 9
ngati osapotshera kudzinga, akwatibwe: kuti tshiri tsha-
bwino ku kwatibwa kopambana ku psa. Koma kwa 10
akukwata diuza, *e* si ndine, koma Mwini, Kuti nkazi
sakatshoka kwa mamuna watshi (koma ndi ngati atshoka, ie 11
akalabe wosakwatibwa, kapenatu aanjanidwe kwa mamuna
watshi); ndimo kuti mamuna sakaleke nkazi watshi. Koma 12
kwa otsala dinena, si Mwini: Ngati mbali modzi apotshera
nkazi wosamvana, ndimo ie aseketswa ku kala nai', wosaleke
ie. Ndimo nkazi emwe apotshera mamuna wosamvana, 13
ndimo ie aseketswa ku kala ndi ie, wosaleke mamuna watshi.
Kuti mamuna wosamvana ayeretsedwa mwa nkazi, ndimo 14
nkazi wosamvana ayeretsedwa mwa mbali: kapena ana anu
anali osätsuka; koma tsopano ali oyera. Koma ngati 15
wosamvana atshoka, atshoke: mbali kapena mlongo osali
pansi pa umpawi m' kotere: koma Mulungu waitana ife m'
ntendere. Kuti bwanje udziwa, O nkazi, ngati udzapulu- 16
mutsa mamuna wako? kapena bwanje udziwa, O mamuna,
ngati udzapulumutsa nkazi wako? Koka, monga Mwini 17
wapatsa ku antu onse, monga Mulungu waitana onse, tshoi-
ntsho aende. Ndimo tshointsho diuza m' maeklesia onse.
Kodi muntu modzi waitanidwa kudulidwa? wosakale 18
wosadulidwa. Kodi modzi anaitanidwa m' kusadula?
wosadulidwe. Kudula kuli tshabe, ndi kusadula kuli 19
tshabe; koma kusunga kwa mau a Mulungu. Antu onse 20
akale m' kuitana kumene mwa komwe anaitanidwa. Kodi 21
unaitanidwa uli kapolo? usasamala kwa iwo: koma ngati
udziwa ku kala waufulu, utshita *iwo* kopambana. Kuti ie 22
emwe anaitanidwa m' Mwini, ali kapolo, ali waufulu wa

Mwini: modzimodzi ie emwe anaitanidwa, ali waufulu, ali
23 kapolo wa Kristu. Munagulidwa ndi ntengo; musakala
24 akapolo a antu. Abali, antu onse, mwa komwe anaitanidwa,
momo akale ndi Mulungu.
25 Ndimo ndi aweta sindipotshera mau a Mwini: koma dipatsa
kuweruza kwanga, monga modzi emwe walandira nsisi kwa
26 Mwini ku kala wamvanu. Ndimo diganiza kuti tshimene
tshiri tshabwino ndi tshifukwa tsha nsoni yatsopano, kuti
27 tshiri tshabwino kwa muntu ku kala monga ali. Kodi
umangidwa kwa nkazi? usafuna ku masulidwa. Kodi
28 umasulidwa kwa nkazi? usafuna nkazi. Koma ndi ngati
ukwata, usanatshimwa; ndimo ngati tshiweta tshikwatibwa,
sitshinatshimwa. Koma otere adzapotshera sautso m' nyama:
29 ndimo dikaianja inu. Koma tshimene dinena, abali, ntawi
ifupikitswa, kuti kwa ntawi yatsopano adya omwe ali ndi
30 akazi angokala monga ngati analibe; ndimo adya omwe
alira misozi, monga ngati sanalira misozi; ndimo adya omwe
asekera, monga ngati sanasekera; ndimo adya omwe agula,
31 monga ngati sanapotshera; ndi adya omwe atshita ndi dziko,
monga sikusakaza ilo: kuti makalidwe a dziko limene apita.
32 Koma difuna inu ku kala aufulu kwa maganizo. Ie emwe
ali wosakwata ali woyang'anira kwa zintu za Mwini, bwanje
33 angoseketsa Mwini: koma ie emwe ali wokwata ali woya-
ng'anira kwa zintu za dziko, bwanje angosekeretsa nkazi
34 watshi. Ndimo kulipo kusiana anso mwa nkazi ndi tshiweta.
Ie emwe ali wosakwatibwa ali woyang'anira kwa zintu za
Mwini, kuti angokala woyera m' tupi ndi m' nzimu: koma
ie emwe ali wokwatibwa ali woyang'anira kwa zintu za
35 dziko, bwanje angoseketsa mamuna watshi. Ndimo tshimene
dinena kwa kupindula kwanu; si kuti dingoponya kwekwe
pa inu, koma kwa tshomwe tshiri tshoyang'anika, ndi kuti
36 mungoimirira pa Mwini kopanda kubaluka. Koma ngati
muntu modzi aganiza kuti adzitangata sikoyang'anika kwa
tshiweta *tshamwanankazi* tshatshi, ngati anapita unamwali
watshi, ndimo ngati kufunidwa tshointsho kufuna, atshite
37 tshomwe afuna; wosatshimwa; akwatane. Koma ie emwe
aima kolimbika m' ntima watshi, kupotshera kufunidwa
kulibe, koma ali ndi mpamvu monga ndi kufuna kwatshi,
ndimo wayerekeza tshimene muntima watshi, ku sunga
tshiweta *tshamwanankazi* tshatshi, adzatshita bwino.
38 Tshointsho pomwe inde ie emwe apatsa tshiweta *tshamwana-
nkazi* tshatshi m' kukwatibwa atshita bwino; ndi iemwe

wosatshipatsa m' kukwatibwa adzatshita bwino kopambana.
Nkazi amangidwa kwa ntawi yeitali monga mamuna watshi 39
akala ndi moyo; koma ngati mamuna anafa, ali wamasuka
ku kwatibwa kwa emwe afuna; koka m' Mwini. Koma ali 40
wosekera kopambana ngati akalabe monga ali, pambuiu
kuweruza kwanga: ndimo diganiza kuti inso diri ndi Nzimu
wa Mulungu.

Ndimo ndi zintu zotsiridwa kwa mafano: Tidziwa kuti 8
tonse tipotshera kudziwa. Kudziwa kutupitsa, koma
kukonda kumanga. Ngati muntu modzi aganiza kuti 2
adziwa kantu, wosadziwa kosuntira monga akanadziwa;
koma ngati muntu modzi akonda Mulungu, ie enso adziwi- 3
dwa ndi ie. Ndimo ndi kudia kwa zintu zotsiridwa kwa 4
mafano, tidziwa kuti palibe fano liri *kantu* m' dziko, ndimo
kuti palibe Mulungu koma modzi. Kuti ngati iripo yomwe 5
itshedwa milungu, kapena m' mwamba kapena pansi; monga
iripo milungu yambiri, ndi eni ambiri; kosuntira kwa ife 6
alipo Mulungu modzi, Atate, ndi emwe ziri zintu zonse, ndi
ife kwa ie; ndi Mwini modzi, Yesu Kristu, mwa emwe ziri
zintu zonse, ndi ife mwa ie. Koma mwa antu onse kusali 7
kudziwa kumene: koma ena, kuzoloweredwa kwa tsopano
ndi fano, adia monga *wa* tshintu tshotsiridwa kwa fano;
ndi kudzidziwitsa kwao kuli kofoka kudetsedwa. Koma 8
nyama siidzabvomereza ife kwa Mulungu: kapena, ngati
sitidia, tisoa; kapena, ngati tidia, titshuruka. Koma 9
yang'anirani kani ndi kantu mpavu imene ya inu, ikala
tshopuntwitsa kwa ofoka. Kuti ngati muntu aona iwe 10
emwe uli ndi kudziwa kukala pa kudia m' tempile la fano,
kodi kudzidziwitsa kwatshi, ngati ali wofoka, kudzalimbikitswa
ku dia zintu zotsiridwa kwa mafano? Kuti mwa kudziwa 11
kwako emwe ali wofoka amwazika, mbali kwa emwe Kristu
anafera. Ndimo tshointsho, kutshimwa pa abali, ndi kulasa 12
kudzidziwitsa kwao ntawi kuli kofoka, mutshimwa pa
Kristu. Ndimo, ngati kudia kukwiitsa mbali wanga, 13
sindidzadia nyama kwa ntawi yonse, kuti sindikwiitsa mbali
wanga.

Kodi sindiri waufulu? kodi sindiri mpostile? kodi sinda- 9
ona Yesu Mwini watu? kodi simuli ntshito yanga m'
Mwini? Ngati kwa ena sindiri mpostile, kosuntira diri 2
nditu kwa inu: kuti tshizindikilo tsha upostile wanga muli
m' Mwini. Kudzikana kwanga kwa awo omwe afunsa ine 3
kuli kumene. Kodi sitiri ndi kwatu ku dia ndi ku mwa? 4

5 Kodi sitiri ndi kwatu ku tsogoza nkazi emwe ali wamvanu,
inde monga apostile ena, ndi abali a Mwini, ndi Kefa?
6 Kapena ine ndeka ndi Barnaba, kodi sitiri ndi kwatu ku
7 leka kutshita? Wankhondo ndani aimirira pa ntawi ina
pa ntengo watshi? ndani aoka munda-wa-mvina, ndimo
wosadia tshobala tsha umo? kapena ndani aeta gulu, ndimo
8 wosadia kwa nkaka wa gulu? Kodi dilankula zintu zi-
menezi pambuiu pa makalidwe a antu? kapena kodi mau
9 sianena anso modzimodzi? Kuti alembedwa m' mau a
Moses, Usapunamiza ng'ombe ntawi ikulunga dzintu. Kodi
10 kuli kwa ng'ombe kuti Mulungu ayang'anira, kapena
aanena konse kwa ife? Inde, kwa ife analembedwa:
tshifuka ie akusa akanakusa m' kulingalira, ndimo ie emwe
akulunga, *akanakulunga* m' kulingalira kwa kugawana.
11 Ngati tinabzala kwa inu zintu zanzimu, kodi tshiri tshintu
12 tshatshikuru ngati tidzatema zintu zanyama zanu? Ngati
ena agawana ndi kwatshi *kumene* pa inu, kodi si ife kopa-
mbana? Koma sitinatshita ndi kwatu kumene; koma
timva zintu zonse, kuti sitingopanga kutshedwa kwa ivangeli
13 wa Kristu. Kodi simudziwa kuti awo omwe aimirira ndi
zintu zoyera adia *ndi* zintu za tempile, *ndi* awo omwe
alindira pa katshisi apotshera kugawana kwao ndi katshisi?
14 Inde tshointsho Mwini nauza kuti awo omwe auza ivangeli
15 akakala ndi moyo ndi ivangeli. Koma datshita ndi palibe
za zintu zimenezi: ndimo sindilemba zintu zimenezi kuti
tshingotshitidwa tshotere m' kwa ine: kuti *tshinali* bwino
kwa ine ku fa, kopambana kuti muntu modzi akapanga
16 kwa tshabe kupambana kwanga. Kuti ngati diuza ivangeli,
sindipotshera kantu ku pambana nako; kuti kufunira kui-
kidwa pa ine; kuti tshaipa tshiri kwa ine, ngati sindiuza
17 ivangeli. Kuti ngati ditshita tshimene tsha kufuna kwanga,
18 dipotshera sekeretso: koma ngati si kwa kufuna kwanga,
dipotshera udindo umvanidwa kwa ine. Ndimo tshiani tshiri
sekeretso langa? Kuti, ntawi diuza ivangeli, dingopanga
ivangeli wopanda ntengo, monga kuti sikutshita kwa kudzaza
19 kwanga m' ivangeli. Kuti ngati dinamasulidwa kwa *antu* onse,
dinadzitenga pansi pa mpawi kwa onse, kuti dinangopindula
20 kopambana. Ndimo kwa Ayuda dinakala monga Myuda,
kuti dinangopindula Ayuda; kwa awo omwe ali pansi pa mau,
monga pansi pa mau, sindiri ine ndeka pansi pa mau, kuti
21 dinangopindula awo omwe ali pansi pa mau; kwa omwe ali
opanda mau, monga wopanda mau, sindiri wopanda mau kwa

Mulungu, koma pansi pa mau kwa Kristu, kuti dinangopi-
ndula awo omwe ali opanda mau. Kwa ofoka dinakala 22
wofoka, kuti dinangopindula ofoka: dakala zintu zonse kwa
antu onse, kuti ndi zifukwa zonse dingopulumutsa ena.
Ndimo ditshita zintu zonse kwa ivangeli, kuti dingokala 23
wogawana anzao wa ilo. Kodi simudziwa kuti awo omwe 24
atamanga m' kutamanga, onse atamanga, koma modzi ala-
ndira sekeretso? Inde tshointsho tamangani, kuti mungo-
fika. Ndimo antu onse omwe ayesa m' masewero adzi- 25
weruza m' zintu zonse. Ndimo *natshita iko* ku landira
tshisoti tshotshuka tshobvunda; koma ife sitshobvunda.
Ndimo tshointshi ditamanga, monga si kosalimbika; tsho- 26
intshi dimenya, monga sikumenya mlengalenga: koma 27
ditundudza tupi langa, nditenga ilo m' umpawi: kani ndi
kantu, pambuiu kuti dauza kwa ena, ine ndeka dikataiidwa.

Kuti sindifuna inu, abali, ku kala opulukira, bwanje kuti 10
atatu atu onse anali pansi pa ntambo, ndi onse napita mwa
nyanja; ndi onse anabapatizidwa kwa Moses mutambo ndi 2
m' nyanja; ndimo onse anadia kudia kumene kwanzimu; 3
ndimo onse anamwa kumwa kumene kwanzimu: kuti 4
anamwa ndi tantwe lanzimu lomwe linatsata awo: ndimo
tantwe linali Kristu. Koma ndi unyinji wa awo Mulungu 5
wosasekera bwino: kuti anagwetsedwa m' tshipululu.
Koma zintu zimenezi zinali masonyezo atu, monga kuti 6
sitikafuna pa zintu zoipa, monga awo onso anafuna. Kapena 7
musakala opembedza mafano, monga anali ena a awo;
monga alembedwa, Antu nakala pansi ku dia ndi ku mwa,
nauka ku sewera. Kapena sititshite dama, monga ena a 8
awo natshita, nagwa m' siku limodzi mazousan makumi
awiri ndi atatu. Kapena sitiyese Mwini, monga ena a awo 9
nayesa, namwazika ndi zinjoka. Kapena musandandaula, 10
monga ena a awo nandandaula, namwazika ndi womwaza.
Koma zintu zimenezi zinafika pa awo monga sonyezo; 11
ndimo nazilembedwa kwa kupunzira kwatu, pa omwe nsonga
za magonero zafika. Mwa kuti ie emwe aganiza aima 12
asamale kani agwa. Kunagwira inu kulibe kuyesa, koma 13
kotere monga muntu adziwa ku mva: koma Mulungu ali
wamvanu, emwe sadzaleka inu ku yesedwa kopambana komwe
muli ndi mpamvu; koma ndi kuyesa adzapanga anso njira
ya kupulumuka, kuti mungokala ndi mpamvu ku mvabe iko.

Mwa kuti, okondedwa anga, tawani kupembedza mafano. 14
Dinena monga kwa antu a nzeru; weruzani inu ndi tshomwe **15**

16 dinena. Tshiko tsha kudalitsa tshomwe tidalitsa, kodi
sikuli unzatshi wa mwazi wa Kristu? Nkate womwe tiswa,
17 kodi siuli unzatshi wa tupi la Kristu? kuona kuti ife, tomwe
tiri ambiri, tiri nkate umodzi, tupi limodzi: kuti ife tonse
18 tigawa kwa nkate umodzi. Yang'anirani Sirayeli pambuiu
pa nyama: kodi awa omwe adia zinsembe siali anz*atshi* a
19 katshisi? Ndimo dinena tshiani? kuti tshintu tshotsiridwa
kwa mafano tshiri kantu, kapena kuti fano liri kantu?
20 Koma *dinena*, kuti zintu zomwe Mitundu itsira, itsira kwa
ademon, ndimo si kwa Mulungu: ndimo sindifuna kuti
21 mukala anz*ao* a ademon. Musadziwa ku mwa tshiko tsha
Mwini, ndi tshiko tsha ademon: musadziwa ku gawa ndi
22 gome la Mwini, ndi gome la ademon. Kapena kodi tiputa
Mwini kwa nsanje? kodi tiri olimba opambana ie?
23 Zintu zonse ziri zamau; koma zintu zonse zosali zopi-
ndulira. Zintu zonse ziri zamau; koma zintu zonse zosa-
24 manga. Palibe modzi afune kwatshi, koma *ubwino* wa
25 woiandikilo watshi. Tshintu tshomwe tshigulitsidwa m' malo
opera nyama, mudia, kufunsa palibe funso kwa kudzidzi-
26 witsa; kuti dziko liri la Mwini, ndi kudzaza kwa ilo.
27 Ngati modzi wa awo omwe osamvana aitana inu *kwa kudia*,
ndimo mufuna ku enda; tshomwe tshiikidwa patsogolo
pa inu, mudia, kufunsa palibe funso kwa kudzidziwitsa.
28 Koma ngati muntu modzi anena kwa inu, Tshimene tshatsiri-
dwa m' nsembe, musadia, kwa iemwe nasonyeza itsho, ndi
29 kwa kudzidziwitsa: kudzidziwitsa, dinena, si kwako, koma
kwa wina; kuti bwanje ufulu wanga uweruzidwa ndi kudzi-
30 dziwitsa kwina? Ngati ine ndi kufatsa digawa, bwanje
dinenedwa koipa ndi tshidya kwa tshomwe dinena tsha-
31 koma? Ndimo kapena mudia, kapena mumwa, kapena
tshintu tshomwe mutshita, tshitani zonse kwa kupambana
32 kwa Mulungu. Musapatsa tshifukwa tsha kupuntwa, ka-
pena kwa Ayuda, kapena kwa Agrike, kapena kwa eklesia
33 la Mulungu: inde monga ine enso disekeretsa antu onse
m' zintu zonse, sikufuna kupindula kwanga, koma *kupindula*
11 kwa ambiri, kuti angopulumutsidwa. Kalani ofanizira a
ine, inde monga diri inso wa Kristu.
2 Ndimo ditama inu kuti mukumbukila ine m' zintu zonse,
ndi mugwira kolimba miambi, inde monga dinapereka iyo
3 kwa inu. Koma difuna inu ku dziwa, kut mutu wa amuna
onse uli Kristu; ndi mutu wa nkazi uli mamuna; ndi mutu
4 wa Kristu uli Mulungu. Amuna onse kupempera kapena

kulosa, ali ndi mitu yao yovundikidwa, anyoza mitu yao.
Koma akazi onse kupempera kapena kulosa ndi mitu yao 5
yosapimbidwa anyoza mitu yao: kuti tshiri tshintu tshi-
modzi ndi tshomwe monga ngati anametedwa. Kuti ngati 6
nkazi wosapimbidwa, leka ie enso ku sengedwa: koma ngati
ali manyazi kwa nkazi ku sengedwa kapena ku metedwa, leka
ie ku pimbidwa. Kuti mamuna nditu sakanapotshera mutu 7
watshi wopimbidwa, mwa kuti ali fanizo ndi kupambana
kwa Mulungu: koma nkazi ali kupambana kwa mamuna.
Kuti mamuna wosali kwa nkazi; koma nkazi kwa mamuna: 8
kuti kapena mamuna sanapangidwa tshifuka tsha nkazi; koma 9
nkazi tshifuka tsha mamuna: kwa tshifuka tshimene nkazi 10
akanapotshera *tshizindikilo tsha* mpamvu pa mutu watshi,
tshifuka tsha anjelo. Koma kapena nkazi wosali wopanda 11
mamuna, kapena mamuna wopanda nkazi, m' Mwini. Kuti 12
monga nkazi ali kwa mamuna, tshointsho onso mamuna ali
ndi nkazi; koma zintu zonse ziri kwa Mulungu. Weruzani 13
mwa inu noka: kodi kuli bwino kuti nkazi apempera kwa
Mulungu wosapimbidwa? Kodi inde makalidwe oka osa- 14
punzitsa inu, kuti, ngati mamuna ali ndi tsisi lalitali, kuli
kunyoza kwa ie? Koma ngati nkazi ali ndi tsisi lalitali, 15
kuli kupambana kwa ie: kuti tsisi latshi lipatsidwa kwa ie
kwa tshovundikila. Koma ngati muntu modzi aenedwa ku 16
kala wandeu, sitipotshera makalidwe otere, kapena maeklesia
a Mulungu.

Koma m' kupatsa inu kuuza kumene, sinditama inu, kuti 17
musong'kana si kwa ubwino wopambana koma kwa kwaipa
kopambana. Kuti poiamba pa onse, ntawi musong'kana 18
m' eklesia, dimva kuti magawano akala mwa inu; ndimo
dikumvana kwa pande. Kuti akanakala anso zinjiru mwa 19
inu, kuti awo omwe asimbidwa angosonyezedwa mwa inu.
Ndimo ntawi musong'kanitsana, sikulikuta ku dia ngonero 20
wa Mwini: kuti m' kudia kwanu onse atenga patsogolo pa 21
*ena* migonero yao; ndimo modzi amva njala, ndi wina
aledzera. Tshiani? kodi simupotshera nyumba ku dia ndi 22
ku mwa mwa *izo*? kapena kodi munyoza eklesia la Mulungu,
ndi mupatsa manyazi ku awo omwe alibe? Tshiani didza-
nena kwa inu? Kodi didzatama inu m' tshimene? Sindi-
tama inu. Kuti dinalandira kwa Mwini tshomwe enso 23
dinapereka kwa inu, bwanje kuti Mwini Yesu m' usiku
momwe anazondedwa natenga nkate; ndimo ntawi ananena 24
tshakoma, nauswa, nati, Umene uli tupi langa, womwe uli

kwa inu: tshimene tshitani m' kukumbutsa kwa ine.
25 Tshointsho onso tshiko, pambuiu ngonero, kuti, Tshiko
tshimene tshiri kupangana kwatsopano m' mwazi wanga:
tshimene tshitani, monga ntawi zambiri monga mumwa,
26 m' kukumbutsa kwa ine. Kuti monga ntawi zambiri monga
mudia nkate umene, ndi mumwa tshiko, musonyeza imfa ya
27 Mwini kwa ntawi afika. Mwa kuti emwe adzadia nkate
kapena adzamwa tshiko tsha Mwini kosaenera, adzakala
28 wotshimwa wa tupi ndi wa mwazi za Mwini. Koma muntu
adziyese, ndi tshointsho adie kwa nkate, ndi amwe kwa
29 tshiko. Kuti iemwe adia ndi amwa, adia ndi amwa ku-
30 weruza kwa ie eka, ngati wosadziwitsa tupi. Kwa tshifukwa
tshimene ambiri mwa inu ali ofoka ndi odwala, ndi si
31 owereng'jeka agona. Koma ngati tinadziwitsa ife toka,
32 sitikaweruzidwa. Koma ntawi tiweruzidwa, tilangidwa ndi
33 Mwini, kuti sitingosutsidwa ndi dziko. Mwa kuti, abali anga,
34 ntawi musong'kana ku dia, lindanani. Ngati muntu modzi
amva njala, adie kwatshi; kuti kusong'kana kwanu kusali
kwa kuweruza. Ndimo zotsala didzakonzetsa ntawi difika.

12 Ndimo ndi *zaulere* zanzimu, abali, sindifuna inu ku kala
2 opulukira. Mudziwa kuti ntawi munali Mitundu muna-
sotsheretswa kwa mafano adya osadziwa ku lankula, monga
3 munangotsogozwa. Mwa kuti dipatsa inu ku dziwa,
kuti palibe muntu kulankula m' Nzimu wa Mulungu anena,
Yesu ali wotukwanidwa; ndimo palibe muntu adziwa
ku nena, Yesu ali Mwini, koma m' Nzimu Woyera.

4 Koma alipo masiano a zaulere, koma Nzimu umodzi.
5 Ndimo alipo masiano a maimiriro, ndi Mwini modzi.
6 Ndimo alipo masiano a matshito, koma Mulungu modzi,
7 emwe atshita zintu zonse mwa onse. Koma kwa onse
8 kupatsidwa kusonyeza kwa Nzimu ku pindula nako. Kuti
kwa modzi kupatsidwa mwa Nzimu mau a nzeru; ndi kwa
9 wina mau a kudziwa, kwa Nzimu umodzi: kwa wina mvanu,
m' Nzimu umodzi; ndi kwa wina zaulere za matshiritso, m'
10 Nzimu umodzi; ndi kwa wina matshito a zimpamvu; ndi
kwa wina kulosa; ndi kwa wina madziwitso a mizimu: kwa
wina mitundu *ina* ya maliu; ndi kwa wina kusanduka kwa
11 maliu: koma zonse zimenezi utshita Nzimu umodzi ndi
womwe, kugawa kwa onse koanjanitswa inde monga ufuna.

12 Kuti monga tupi liri limodzi, ndimo liri ndi dziwalo
dzambiri, ndi dziwalo dzonse dza tupi, dziri dzambiri, dziri
13 tupi limodzi; tshointsho onso ali Kristu. Kuti m' Nzimu

umodzi ife tonse tinabapatizidwa m' tupi limodzi, kapena
Ayuda kapena Agrike, kapena akapolo kapena aufulu; ndi
onse tinamwetsedwa ndi Nzimu umodzi. Kuti tupi siliri 14
tshiwalo tshimodzi, koma dzambiri. Ngati pazi lidzanena, 15
Tshifuka sindiri dzanja, sindiri la tupi; ndimo siliri si la
tupi. Ndimo ngati kutu lidzanena, Tshifuka sindiri diso, 16
sindiri la tupi; ndimo siliri si la tupi. Ngati tupi lonse
linali diso, kumva kunali kuti? Ngati lonse linali kumva, 17
kunung'ka kunali kuti? Koma tsopano Mulungu waika 18
dziwalo dzonse dza idzo m' tupi, inde monga kunasekeretsa
ie. Ndimo ngati dzinali dzonse tshiwalo tshimodzi, tupi 19
linali kuti? Koma tsopano dziri dziwalo dzambiri, koma 20
tupi limodzi. Ndimo diso losadziwa ku nena kwa dzanja, 21
Sindiri ndi kufunidwa ndi iwe: kapena anso mutu kwa
mapazi, Sindiri ndi kufunidwa ndi inu. Iai, kwambiri 22
kopambana, dziwalo dzidya dza tupi dzomwe dzienedwa
ku kala dzofoka dzopambana dzifunidwa: ndimo *mapande* 23
adya a tupi, omwe tiganiza kukala aulemu ang'ono opa-
mbana, pa amene tiika ulemu wambiri wopambana; ndi
*mapande* osakonzetsa atu apotshera kukonzetsa kopambana;
koma *mapande* okonzetsa atu osali ndi kufunidwa: koma 24
Mulungu nawiritsa tupi pamodzi, kupatsa ulemu wambiri
wopambana kwa *pande* limene lomwe linapanda; kuti 25
kusakakala kugawana m' tupi; koma *kuti* dzïwalo dzïkapo-
tshera kuyang'anira kumodzi tshimodzi kwa tshina.
Ndimo kapena tshiwalo tshimodzi tshimva, dziwalo dzonse 26
dzimva natsho; kapena tshiwalo *tshimodzi* tshipamba-
nitsidwa, dziwalo dzonse dzisekera natsho. Koma muli tupi 27
la Kristu, ndi koanjanitswa dziwalo dza ilo. Ndimo 28
Mulungu waika ena m' eklesia, poiamba apostile, patshiwiri
aprofeti, patshitatu apunzitsi, pomwe zimpamvu, pomwe
zaulere za matshiritso, matangato, maweruzo, mitundu *ina*
ya maliu. Kodi onse ali apostile? kodi onse ali aprofeti? 29
kodi onse ali apunzitsi? kodi onse ali *akutshita a* zimpamvu?
kodi onse apotshera zaulere za matshiritso? kodi onse 30
alankula ndi maliu? kodi onse asandutsa? Koma funani 31
kolimba zaulere zopambana. Ndimo njira yabwino yopa-
mbana disonya kwa inu.

Ngati dilankula ndi maliu a antu ndi a anjelo, koma 13
sindipotshera kukonda, dikala nkua woomba, kapena simbale
lolira. Ndimo ngati dipotshera *tshaulere tsha* kulosa, ndi- 2
dziwa kusadziwika zonse ndi kudziwa konse; ndimo ngati

dipotshera mvanu wonse, monga kuti ku sunta mapiri, koma
3 sindiri ndi kukonda, diri tshabe. Ndimo ngati dipatsa
zintu zanga zonse ku eta *osauka*, ndimo ngati dipatsa tupi
langa ku otshedwa, koma sindiri ndi kukonda, sindipindula
4 kantu. Kukonda kumva kutali, *ndimo* kuli kokoma;
5 kukonda kusadana; kukonda kusadzibalawaza, kusatu-
pitswa, kusadzitangata kosaenera, kusasaka kwatshi, kusa-
6 putidwa, kusaganiza ndi mpulupulu; kusasekera m' kusa-
7 deka, koma kusekera ndi nteradi; kumva zintu zonse,
kumvana ndi zintu zonse, kulingalira ndi zintu zonse, ku-
8 mvabe zintu zonse. Kukonda kusaperewera palibe ntawi:
koma kapena *alipo* maloso, adzatshotsedwa; kapena *alipo*
maliu, adzaleka; kapena *kulipo* kudziwa, kudzatshotsedwa.
9, 10 Kuti tidziwa m' pande, ndimo tilosa m' pande: koma ntawi
kumene komwe kuli kwakuta kunafika, komwe kuli m' pande
11 kudzatshotsedwa. Ntawi dinali mwana, dinalankula monga
mwana, dinamva monga mwana, dinaganiza monga mwana:
tsopano kuti dikala mamuna, dinatshotsa zintu zaubwana.
12 Kuti tsopano tiona m' karirole, kodetsa; koma pomwe nkope
ndi nkope: tsopano didziwa m' pande; koma pomwe didza-
13 dziwa inde monga anso dadziwidwa. Koma tsopano zikalabe
mvanu, kulingalira, kukonda, zitatu zimenezi; koma kwa-
kukuru kopambana kwa izo kuli kukonda.

14 Tsatani kukonda; kosuntira funani kolimbika *zaulere*
2 zanzimu, koma kopambana kuti mungolosa. Kuti iemwe
alankula m' liu alankula si kwa antu, koma kwa Mulungu;
kuti palibe muntu adziwitsa; koma m' nzimu alankula
3 kusadziwika. Koma iemwe alosa alankula ndi antu kumanga,
4 ndi kusangalatsa, ndi kuiwaza. Iemwe alankula m' liu
adzimanga; koma iemwe alosa amanga eklesia. Koma
difuna inu nonse ku lankula ndi maliu, koma kopambana
5 kuti mukalosa: ndimo wang'kuru ali iemwe alosa wopa-
mbana emwe alankula ndi maliu, kani asandutsa, kuti eklesia
6 lingolandira kumanga. Koma tsopano, abali, ngati difika
kwa inu kulankula ndi maliu, didzapindula inu bwanje,
kani dilankula ndi inu kapena ndi njira ya kusonyeza,
kapena ya kudziwa, kapena ya kulosa, kapena ya kupunzitsa?
7 Inde zintu zopanda moyo, kupatsa liu, kapena mlumbwi
kapena harpe, ngati zosapatsa kusiana mwa anamalowe,
bwanje tshidzadziwidwa tshiani tshiombedwa pa mlumbwi
8 kapena tshiombedwa pa harpe? Kuti ngati lipenga lipa-
tsa liu losadziwika, ndani adzadzikonza kwa nkondo?

Tshointsho onso inu, kani mutshula ndi lilume kulankula 9
kopepuka ku dziwitsidwa, bwanje tshidzadziwidwa tshiani
tshilankulidwa? kuti mudzalikulankula m' mlengalenga.
Kunali, kungokala, mitundu yambiri ya maliu m' dziko, 10
ndimo palibe umodzi uli wopanda tantauzo. Ngati pomwe 11
sindidziwa tantauzo la liu, didzakala kwa iemwe alankula
mbaribari, ndi iemwe alankula adzakala mbaribari kwa
ine. Tshointshi inso inu, tshifuka muli atshangu a 12
*zaulere* zanzimu, funani kuti mungotshurutsa kwa kumanga
kwa eklesia. Mwa kuti ie emwe alankula m' liu apempere 13
kuti angosandutsa. Kuti ngati dipempera m' liu, nzimu 14
wanga upempera, koma kudziwa kwanga kuli kopanda
dzobala. Ndimo tshiri tshiani? Didzapempera ndi nzimu, 15
ndimo didzapempera ndi kudziwa anso: didzaimba ndi
nzimu, ndimo didzaimba ndi kudziwa anso. Kani ngati 16
udala ndi nzimu, bwanje iemwe adzaza malo a wosapunzitsa
adzanena Amen pa kunena tshakoma kwako, kuona kuti
wosadziwa tshomwe unena? Kuti iwe nditu upatsa tsha- 17
koma bwino, koma wina wosamangidwa. Dinena tshakoma 18
kwa Mulungu, dilankula ndi maliu kopambana inu nonse:
koma m' eklesia difuna ku lankula mau asanu ndi kudziwa 19
kwanga, kuti dingopunzitsa ena anso, kopambana mau
mazousan kumi m' liu.

Abali, musakala ana m' muwongo: koma m' madano kalani 20
makanda, koma m' muwongo kalani akuru. M' mau 21
tshilembedwa, Ndi antu a maliu ena ndimo ndi milomo ya
ena didzalankula ndi antu amene; ndimo inde si tshointshi
adzamva ine, ati Mwini. Mwa kuti maliu ali kwa 22
tshizindikilo, si kwa awo omwe amvana, koma kwa
osamvana: koma kulosa *kuli kwa tshizindikilo*, si kwa
osamvana, koma kwa awo omwe amvana. Ndimo ngati 23
eklesia lonse lisong'kanidwa, ndi onse alankula ndi maliu,
ndimo aloa antu osapunzitsa kapena osamvana, kodi
sadzanena kuti muli amisala? Koma ngati onse alosa, 24
ndimo aloa modzi wosamvana kapena wosapunzitsa,
asulumulidwa ndi onse, aweruzidwa ndi onse; zakutseri za 25
ntima watshi zisonyezedwa; ndimo tshointsho adzagwa pa
nkope yatshi nadzapembedza Mulungu, kuuza kuti Mulungu
ali mwa inu nditu.

Ndimo tshiri tshiani, abali? Ntawi musong'kana, onse 26
apotshera salmo, apotshera kupunzitsa, apotshera kusonyeza,
apotshera liu, apotshera kusandutsa. Zintu zonse zitshitidwe

27 kwa kumanga. Ngati muntu modzi alankula m' liu, *kukale* ndi
awiri, kapena pa ambiri opambana atatu, ndi *kumene* m'
28 kundandalika; ndimo modzi asandutse: koma ngati palibe
wosandutsa, akale tshete m' eklesia; ndimo alankule kwa ie
29 eka, ndi kwa Mulungu. Ndimo aprofeti alankule *ndi* awiri
30 kapena atatu, ndi ena adziwitse. Koma ngati kusonyeza
kupangidwa kwa wina kukala pafupi, woiamba akale tshete.
31 Kuti inu nonse mudziwa ku losa modzi ndi modzi, kuti onse
32 mungopunzira, ndi onse mungosangalatsidwa; ndi mizimu
33 ya aprofeti iri pansi pa aprofeti; kuti Mulungu siali
*Mulungu* wa kusokaniza, koma wa ntendere; monga m'
maeklesia onse a oyera.
34 Akazi akale tshete m' maeklesia: kuti sikuloledwa kwa
awo ku lankula; koma akale pansipa, monga mau unso
35 anena. Ndimo ngati afuna ku punzira kantu, afunse amuna
ao kwao: kuti ali manyazi kwa nkazi ku lankula m' eklesia.
36 Tshiani? kodi kwa inu kuti mau a Mulungu anaturuka?
kapena kodi anafika kwa inu noka?
37 Ngati muntu modzi aganiza ie eka ali mprofeti, kapena
wanzimu, atenge kudziwa ndi zintu zomwe dilemba kwa
38 inu, kuti ziri mau a Mwini. Koma ngati muntu modzi ali
wopulukira, akale wopulukira.
39 Mwa kuti, abali anga, funani kwambiri ku losa, ndimo
40 musaletsa ku lankula ndi maliu. Koma zintu zonse zitshi-
tidwe kolinganira ndi mwa kundandalika.
15 Koma didziwitsa inu, abali, ivangeli womwe dinauza kwa
2 inu, womwe enso munalandira, mwa kuti inso muima, ndi
womwe enso mupulumutsidwa; *didziwitsa*, *dinena*, ndi mau
anje dinauza iwo kwa inu, ngati mugwira iwo kolimba, kani
3 munamvana kopanda tshifukwa. Kuti dinapereka kwa inu
poiamba kwa onse tshimene tshomwe enso dinalandira,
bwanje kuti Kristu anafera kwa zoipa zatu kwa malemba;
4 ndi kuti anaikidwa m' mwanda; ndimo kuti waukitsidwa pa
5 siku latshitatu kwa malemba; ndi kuti anadzisonya kwa
6 Kefa; pomwe kwa kumi ndi awiri; ndimo nadzisonya kwa
opambana mazana asanu pa ntawi imodzi, a omwe unyinji
7 akala kwa tsopano, koma ena anagona; ndimo nadzisonya
8 kwa Yakobi; pomwe kwa apostile onse; ndimo pambuiu pa
onse, monga kwa modzi wabadwa si mwa ntawi yabwino,
9 nadzisonya kwa ine enso. Kuti diri wang'ono wopambana
wa apostile, kuti sindiri woenera ku tshedwa mpostile,
10 tshifuka dinazunza eklesia la Mulungu. Koma ndi kufatsa

kwa Mulungu diri emwe diri: ndimo kufatsa kwatshi komwe
kunapatsidwa kwa ine kusanapezedwa tshabe; koma
dinatshita kotshuruka kopambana awo onse: kosuntira si
ine, koma kufatsa kwa Mulungu komwe kunali ndi ine.
Ndimo kapena ine kapena awo, tshointsho tiuza, ndi 11
tshointsho munamvana.

Ndimo ngati Kristu auzidwa kuti anaukitswa kwa akufa, 12
bwanje ena mwa inu anena kuti kulibe kuukirira kwa
akufa? Koma ngati kulibe kuukirira kwa akufa, kapena 13
Kristu sanaukitswa: ndimo ngati Kristu wosaukitswa, 14
pomwe kuuza kwanu kuli tshabe, mvanu wanu unso uli
tshabe. Inde, ndimo tipezedwa omariza onama a Mulungu; 15
tshifuka tinamariza ndi Mulungu kuti anaukitswa Kristu:
emwe sanaukitswa, ngati kuli tshointsho kuti akufa osauki-
tsidwa. Kuti ngati akufa osaukitsidwa, kapena Kristu wosa- 16
naukitsidwa: ndimo ngati Kristu sanaukitsidwa, mvanu wanu 17
uli tshabe; muli kosuntira m' zakwaipa zanu. Ndimo awo 18
onso omwe anagona m' Kristu anamwazika. Ngati m' 19
moyo watsopano woka talingalira m' Kristu, tiri a antu onse
okalitsa nsoni opambana.

Koma tsopano Kristu waukitswa kwa akufa, dzobala 20
dzoiamba dza omwe agona. Kuti monga ndi muntu *inadza* 21
imfa, ndi muntu *kunadza* anso kuukirira kwa akufa. Kuti 22
monga m' Adam onse afa, tshointsho onso m' Kristu onse
adzapangidwa amoyo. Koma onse m' kundandalika kwao: 23
Kristu dzobala dzoiamba; pomwe awo omwe ali a Kristu, pa
kusonya kwatshi. Ndimo *idza* nsonga, ntawi adzapereka dziko 24
kwa Mulungu, inde Atate; ntawi anatshotsa kuweruza
konse ndi umwini wonse ndi mpamvu. Kuti akanawertuza, 25
kwa ntawi waika maliwongo atshi onse pansi pa mapazi
atshi. Liwongo lakutungo lomwe lidzatshotsedwa liri imfa. 26
Kuti, Naika zintu zonse pansi pa mapazi atshi. Koma ntawi 27
anena, zintu zonse ziikidwa pansi pa *ie*, kuli koona kuti
ie atsalitswa emwe anaika zintu zonse pansi pa ie. Ndimo 28
ntawi zintu zonse zinaikidwa pansi pa ie, pomwe Mwana
anso ie eka adzaikidwa pansi pa ie emwe anaika zintu zonse
pansi pa ie, kuti Mulungu angokala onse mwa onse.

Kani awa adzatshita tshiani omwe abapatizidwa kwa 29
akufa? Ngati akufa osaukitswa konse, nanga bwanje awo
abapatizidwa kwa awo? bwanje ife enso tiima m' kutse- 30
kerezwa maora onse? Diuza ndi kupambana kumene mwa 31
inu, abali, komwe dipotshera m' Kristu Yesu Mwini watu,

32 difa masiku onse. Ngati pambuiu makalidwe a antu dina-
menyana ndi zirombo pa Feso, tshiani tshipindula ine?
Ngati akufa osaukitswa, tidie ndi timwe, kuti mawa tifa.
33 Musanyengedwa: Unzatshi woipa uipitsa matangato
34 abwino. Ukani kodeka, ndimo musatshimwa; kuti ena sali
ndi kudziwa kwa Mulungu: dilankula *tshimene* ku sunta
inu kwa manyazi.
35 Koma modzi wina adzati, Bwanje akufa aukitswa? ndimo
36 ndi tupi lanje adzafika? Wapusa iwe, tshomwe iwe eka
37 ubzala tshosafulumizwa, kani tshifa: ndimo tshomwe
ubzala, usabzala tupi lomwe lidzakala, koma mpetshe yoka,
38 ingokala ya trigu, kapena ya mtundu wina; koma Mulungu
aipatsa tupi inde monga anasekeretsa ie, ndi kwa mbeu zonse
39 tupi la izo. Nyama zonse siziri nyama zimodzimodzi:
koma iripo *nyama* imodzi ya antu, ndi nyama ina ya ziro-
mbo, ndi nyama ina ya zimbalame, ndi ina ya zinsomba.
40 Ziri inso matupi amwamba, ndi matupi adziko: koma
kupambana kwa amwamba kuli kumodzi, ndi *kupambana*
41 kwa adziko kuli kwina. Kulipo kupambana kumodzi
kwa dzua, ndi kupambana kwina kwa mwezi, ndi
kupambana kwina kwa nyenyezi; kuti nyenyezi imodzi
42 isiana kwa nyenyezi ina m' kupambana. Tshointsho onso
kuukirira kwa akufa. Libzalidwa m' kubvunda; liukitswa
43 m' kusabvunda: libzalidwa m' kunyoza; liukitswa m'
kupambana: libzalidwa m' kufoka; liukitswa m' mpamvu:
44 libzalidwa tupi lamakalidwe; liukitswa tupi lanzimu.
Ngati liri tupi lamakalidwe, liri inso *tupi* lanzimu.
45 Tshointsho onso alembedwa, Muntu woiamba Adam nakala
nzimu wamoyo. Adam wakutungo *nakala* nzimu wakupatsa
46 moyo. Koma limene si liri loiamba lomwe liri lanzimu,
koma limene lomwe liri lamakalidwe; pomwe limene
47 lomwe liri lanzimu. Muntu woiamba ali wa dziko,
48 wantaka: muntu watshiwiri ali wa kumwamba. Monga
ali wantaka, otere ali awo onso omwe ali antaka:
ndimo monga ali wakumwamba, otere ali awo onso omwe
49 ali akumwamba. Ndimo monga tanyamula fanizo la
wantaka, tidzanyamula anso fanizo la wakumwamba.
50 Koma tshimene dinena, abali, kuti nyama ndi mwazi
zosadziwa ku loa m' dziko la Mulungu; kapena kubvunda
51 kusaloa m' kusabvunda. Ona, diuza inu kusadziwika:
52 Sitigona tonse, koma tidzasintanidwa tonse, m' kantawe, m'
kutwanima kwa diso, pa lipenga lakutungo: kuti lipenga

lidzaomba, ndi akufa adzaukitswa akusabvunda, ndimo
tidzasintanidwa. Kuti kubvunda kumene kukanabvala 53
kusabvunda, ndimo lantembo limene likanabvala kusafa.
Koma ntawi kubvunda kumene kudzabvekedwa kusabvunda, 54
ndimo lantembo limene lidzabvekedwa kusafa, pomwe
kudzafika kunena komwe kulembedwa, Imfa imezedwa m'
kupambana. O imfa, kupambana kwako kuli kuti? O 55
imfa, mbola yako iri kuti? Mbola ya imfa iri 56
mpulupulu; ndi mpamvu ya mpulupulu iri mau:
koma tshakoma kwa Mulungu, emwe apatsa ife kupa- 57
mbana mwa Mwini watu Yesu Kristu. Mwa kuti, 58
abali anga okondedwa, kalani kolimbika, kosasunta, ntawi
yonse kutshurutsa mwa ntshito ya Mwini, kudziwa kuti
ntshito yanu siiri tshabe m' Mwini.

Koma ndi song'kanitso kwa oyera, monga dinauza ku 16
maeklesia a Galatiya, tshointsho onso tshitani. Pa dzua 2
loamba la wiki onse a inu aike pa ie, kusungira, monga
angokula, kuti palibe masong'kanitso apangidwe ntawi
difika. Ndimo ntawi difika, emwe mudzasimba ndi 3
maepistola, awo didzatumiza ku nyamula kuanja kwanu kwa
Yerusalem: ndimo ngati tshiri tshabwino kwa ine enso ku 4
muka, adzamuka ndi ine. Koma didzafika kwa inu, ntawi 5
dinapita pakati pa Makedoniya; kuti dipita nditu pakati pa
Makedoniya; koma ndi inu kungokala kuti didzakala, 6
kapena inde didzakala-malimwe, kuti mungoperekeza ine pa
ulendo wanga pomwe dimuka. Kuti sindifuna ku ona inu 7
tsopano ndi njira; kuti dilingalira ku kala ntawi ndi inu,
ngati Mwini alola. Koma didzakala pa Feso kwa 8
Pentekoste; kuti tshitseko tshatshikuru ndi tshotetsa 9
tshitsegulidwa kwa ine, ndimo alipo maliwongo ambiri.

Ndimo ngati Timote adza, onani kuti akale ndi inu 10
wopanda kuopa; kuti atshita ntshito ya Mwini, monga anso
ditshita: ndimo palibe muntu modzi anyoze ie. Koma 11
perekezani ie pa ulendo watshi m' ntendere, kuti angofika
kwa ine: kuti diyang'anira ie ndi abali. Koma monga ndi 12
Apolo mbali, dinapempa ie kwambiri ku dza kwa inu ndi
abali: ndimo sikunali kufuna *kwatshi* konse ku fika tsopano;
koma adzafika ntawi adzali ndi pofatsa.

Dikirani, imani kolimba mumvanu, mudzitangate ofana 13
amuna, kalani olimba. Zonse zomwe mutshita zitshitidwe 14
m' kukonda.

Ndimo dipempa inu, abali (mudziwa nyumba ya Stefana, 15

kuti iri dzobala dzoiamba dza Akaya, ndimo kuti anaika
16 awo oka ku imirira kwa oyera), kuti inu unso mukale pansi
pa otere, ndi kwa onse omwe atangata m' ntshito natshita.
17 Ndimo disekera pa kufika kwa Stefana ndi Fortunato ndi
Akayiko: kuti tshimene tshomwe tshinapanda pa pande lanu
18 anakwanitsa. Kuti nasangalatsa nzimu wanga ndi wanu:
ndimo bvomerezani omwe ali otere.
19 Maeklesia a Asiya autsa inu. Akwila ndi Priska autsa
inu kwambiri m' Mwini, ndi eklesia lomwe liri m' nyumba
20 yao. Abali onse autsa inu. Utsanani ndi kumsomsona
koyera.
21, 22 Utso la ine Paulos ndi dzanja langa loka. Ngati muntu
modzi wosakonda Mwini, akale wotukwanidwa. Mwini
23 adza. Kufatsa kwa Mwini Yesu Kristu kukale ndi inu.
24 Kukonda kwanga kukale ndi inu nonse m' Kristu Yesu.
Amen.

---

EPISTOLA LATSHIWIRI LA PAULOS KWA

# AKORINTE.

1 PAULOS, mpostile wa Kristu Yesu mwa kufuna kwa
Mulungu, ndi Timote mbali watu, kwa eklesia la
Mulungu lomwe liri pa Korinte, ndi oyera onse omwe ali
2 m' Akaya lonse: Kufatsa kwa inu, ndi ntendere kwa
Mulungu Atatu atu ndi Mwini Yesu Kristu.
3 Wodala *akale* Mulungu ndi Atate a Mwini watu Yesu
Kristu, Atate a zinsisi ndi Mulungu wa kusangalatsa konse;
4 emwe asangalatsa ife m' sautso yatu yonse, monga kuti
tingodziwa ku sangalatsa awo omwe ali m' sautso ina, mwa
kusangalatsa ndi komwe ife toka tisangalatsidwa ndi
5 Mulungu. Kuti monga kumva kwa Kristu kutshuruka kwa
ife, inde tshointsho kusangalatsa kwatu unso kutshuruka
6 mwa Kristu. Koma kapena tisautsidwa, kuli kwa kusanga-
latsa ndi kupulumutsa kwanu; kapena ngati tisangalatsidwa,
kuli kwa kusangalatsa kwanu, komwe kutshita m' kumvabe

kolongosola kwa kumva kumene komwe ife enso timva:
ndi kulingalira kwatu kwa inu kuli kolimbika; kudziwa 7
kuti, monga muli ogawana a kumva, tshointsho onso muli a
kusangalatsa. Kuti sitifuna inu ku kala opulukira, abali, 8
ndi sautso yatu yomwe inafika pa *ife* m' Asiya, kuti tinale-
medwa kwambiri, kopambana kwa mpamvu yatu, mwa
ambiri kuti tinalizinga inde wa moyo: inde, ife toka tinali 9
ndi tshulo la imfa mwa ife toka, kuti sitikanamvana mwa
ife toka, koma m' Mulungu emwe aukitsa akufa: emwe 10
anapulumutsa ife mwa imfa yeikuru yotere, ndimo adzapu-
lumutsa: pa emwe ife tinaika kulingalira kwatu kuti
adzatipulumutsa ife enso kosuntira; inu unso kutangatana 11
kwa ife ndi kupempa kwanu; kuti, kwa tshaulere tshinapa-
tsidwa pa ife ndi zifukwa za ambiri, tshakoma tshingopatsi-
dwa ndi antu ambiri kwa ife.

Kuti kupambana kwatu kuli kumene, kumariza kwa 12
kudzidziwitsa kwatu, kuti m' kuyera ndi nteradi za Mulungu,
si m' nzeru zanyama koma m' kufatsa kwa Mulungu,
tinadzitangata m' dziko, ndi kopambana kwa inu. Kuti 13
tilemba si zintu zina kwa inu, kopambana zomwe muwerenga
kapena inde mubvomereza, ndimo dilingalira mudzabvome-
reza kwa nsonga: monga anso munabvomereza ife m' 14
pande, kuti tiri kupambana kwanu, inde monga muli inso
kwatu, m' dzua la Mwini watu Yesu.

Ndimo m' kumvana kumene dinafuna ku dza patsogolo 15
kwa inu, kuti munangopotshera kuanja kwatshiwiri; ndimo 16
ndi inu ku pita m' Makedoniya, ndi inso kwa Makedoniya
ku fika kwa inu, ndimo ndi inu ku perekezedwa pa ulendo
panga kwa Yudeya. Ndimo ntawi dinali ndi ntima 17
tshointsho, kodi dinasonyeza kutembenukatembenuka?
kapena zintu zomwe diyerekeza, kodi diyerekeza kwa nyama,
kuti ndi ine zikakala inde inde ndi iai iai? Koma monga 18
Mulungu ali wamvanu, mau atu kwa inu osali inde ndi iai.
Kuti Mwana wa Mulungu, Yesu Kristu, emwe anauzidwa 19
mwa inu mwa ife, *inde* mwa ine ndi Silvano ndi Timote,
sanali inde ndi iai, koma mwa ie ali inde. Kuti bwanje 20
otshuruka ambiri ali malonjezano a Mulungu, mwa ie ali
inde: ndimo onso mwa ie ali Amen, kwa kupambana kwa
Mulungu mwa ife. Ndimo iemwe alimbikitsa ife ndi inu m' 21
Kristu, nadzosa ife, ali Mulungu; emwe enso anasindikiza 22
ife, na*ti*patsa tshigwiriro tsha Nzimu m' mitima yatu.

Koma diitana Mulungu kwa kumariza pa nzimu wanga, 23

24 kuti ku yanja inu dinaleka ku fika kwa Korinte. Si kuti
tikala ndi umwini pa mvanu wanu, koma tiri akutangata a
2 tshimwemwe tshanu: kuti ndi mvanu muima. Koma
dinayerekeza tshimene ndi ine ndeka, kuti sindikadza anso
2 kwa inu ndi tshisoni. Kuti ngati dipanga inu atshisoni,
ndimo ndani ali iemwe apanga ine wosekera, koma iemwe
3 apangidwa watshisoni ndi ine? Ndimo dinalemba tshintu
tshimene nditu, kani, ntawi dinafika, dikapotshera tshisoni
kwa awo ndi omwe dikanasekera; kuli ndi mvanu ndi inu
nonse, kuti tshimwemwe tshanga tshiri *tshimwemwe* tsha inu
4 nonse. Kuti mwa sautso yambiri ndi kupweteka za ntima
dinalemba kwa inu ndi misozi yambiri; si kuti mukanapa-
ngidwa atshisoni, koma kuti munangodziwa kukonda komwe
dipotshera kopambana kwa inu.
5 Koma ngati wina wapanga tshisoni, wapanga tshisoni, si
kwa ine, koma m' pande (kuti sindilemetsa kotshuruka) kwa
6 inu nonse. Kokwanira kwa modzi wotere kuli kulanga
7 kumene komwe *kunalangidwa* ndi unyinji; monga kuti
kodulitsa mukakululukira ie kopambana ndi ku sangalatsa
ie, kani ndi kantu, modzi wotere akamezedwa ndi tshisoni
8 tshatshi tshambiri. Mwa kuti dipempa inu ku limbikitsa
9 kukonda *kwanu* kwa ie. Kuti kwa nsonga imene enso
dinalemba, kuti dinangodziwa kuyesa kwa inu, ngati muli
10 omvera m' zintu zonse. Koma kwa omwe mukululukira
kantu, di*kululukira* anso: kuti tshomwe enso dakululukira,
ngati dakululukira kantu, kwa inu *dakululukira iko* m'
11 kuona kwa Kristu; kuti palibe kupindula kungopezedwa
pa ife ndi Satana: kuti sitiri opulukira ndi maganizo
atshi.
12 Ndimo ntawi dinafika ku Trowa kwa ivangeli wa Kristu,
ndimo ntawi tshitseko tshinatsegulidwa kwa ine m' Mwini,
13 sindinapotshera kuleka kwa nzimu wanga, tshifuka sindina-
peza Tito mbali wanga: koma kutsazika kwa awo, dina-
14 muka m' Makedoniya. Koma tshakoma kwa Mulungu,
emwe ntawi yonse atsogoza ife m' kupambana m' Kristu,
nasonyeza mwa ife tshonung'kira tsha kudziwa kwatshi m'
15 malo onse. Kuti tiri tshonung'kira tshabwino tsha Kristu
kwa Mulungu, mwa omwe alikupulumutsidwa, ndi mwa
16 omwe alikumwazika; kwa modzi tshonung'kira kwa imfa ku
imfa; kwa wina tshonung'kira kwa moyo ku moyo. Ndimo
17 ndani ali wokwanitsa kwa zintu zimenezi? Kuti sitiri
monga ambiri, kusintana mau a Mulungu: koma monga

ndi nteradi, koma monga ndi Mulungu, m' kuona kwa
Mulungu, tilankula m' Kristu.

Kodi tirikuamba anso kudzibvomereza? kapena kodi 3
tifuna, monga ena, maepistola a kubvomereza ku inu
kapena kwa inu? Muli epistola latu, linalembedwa 2
m' mitima yatu, lidziwidwa ndi liwerengedwa ndi antu
onse; kusonyezedwa kuti muli epistola la Kristu, lina- 3
imiririridwa ndi ife, linalembedwa si ndi inke, koma ndi
Nzimu wa Mulungu wamoyo; si m' magome a mwala,
koma m' magome *omwe ali* mitima ya nyama. Ndimo 4
kumvaua kotere tipotshera mwa Kristu kwa Mulungu:
si kuti tiri okwanitsa ndi ife toka, ku ganiza kantu monga 5
kwa ife toka; koma kukwanitsa kwatu kuli kwa Mulungu;
emwe enso napanga ife okwanitsa monga oimirira a ku- 6
pangana kwatsopano; si a lemba, koma a nzimu: kuti
lemba lipa, koma nzimu upatsa moyo. Koma ngati ku- 7
imirira kwa imfa, m' malemba, *ndi* kunatshekedwa pa
miala, kunadza ndi kupambana, monga kuti ana a Sirayeli
sanadziwa ku yang'anitsa pa nkope ya Moses tshifuka tsha
kupambana kwa nkope yatshi; komwe kunalikupita:
bwanje kopambana kuimirira kwa nzimu sikudzakala ndi 8
kupambana? Kuti ngati kuimirira kwa kusutsa kuli kupa- 9
mbana, kwambiri kopambana kuimirira kwa kudeka ku-
tshurutsa m' kupambana. Kuti nditu tshomwe tshina- 10
pangidwa tshopambana tshosanapangidwa tshopambana
m' tshimene, tshifuka tsha kupambana komwe kutshurutsa.
Kuti ngati tshomwe tshipita *tshinali* ndi kupambana, kwa- 11
mbiri kopambana tshomwe tshitsala *tshiri* m' kupa-
mbana.

Ndimo kuli ndi kulingalira kotere, titshita ndi kulimba 12
kwakukuru kwa kunena, ndimo si monga Moses, *emwe* 13
naika tshopimba pa nkope yatshi, kuti ana a Sirayeli saka-
yang'anitsa pa nsonga ya tshomwe tshinalikupita: koma 14
ntintu zao zinalimbikitswa: kuti kwa siku limene nditu pa
kuwerenga kwa kupangana kwakali tshopimba tshomwe
tshitsala tshosatukulidwa; tshomwe tshitshotsedwa m' Kristu.
Koma kwa siku limene, ntawi Moses awerengedwa, tsho- 15
pimba tshikala pa ntima wao. Koma ntawi adzatembenuka 16
kwa Mwini, tshopimba tshitshotsedwa. Ndimo Mwini ali 17
Nzimu: ndimo pomwe Nzimu wa Mwini uli, *ulipo* ufulu.
Koma ife tonse, ndi nkope yosapimbidwa kubweza monga 18
karirole kupambana kwa Mwini, tisandulizidwa m' fanizo

limodzi kwa kupambana ku kupambana, inde monga kwa
Mwini Nzimu.
4 Ndimo monga tipotshera kuimirira kumene, inde monga
2 tinalandira nsisi, sitifoka: koma tataia zintu zobisa za
manyazi, sikuendaenda m' kutshenjera, kapena sikutosa mau
a Mulungu konyenga; koma ndi kusonyeza kwa nteradi
kudzibvomereza kwa kudzidziwitsa kwa antu onse m' kuona
3 kwa Mulungu. Koma ndimo ngati ivangeli watu uli
wopimbidwa, uli wopimbidwa mwa awo omwe alikumwa-
4 zika: mwa omwe mulungu wa kugonera kumene watseka
maso a mauongo a osamvana, kuti kuwala kwa ivangeli
kwa kupambana kwa Kristu, emwe ali fanizo la Mulungu,
5 kusakaatsha *pa awo.* Kuti tiuza si ife toka, koma Kristu
Yesu monga Mwini, ndi ife toka monga akapolo anu kwa
6 Yesu. Tshifuka ali Mulungu, emwe ananena, Kuunika
kudzawala kwa ndima, emwe anawala m' mitima yatu, ku
patsa kuwala kwa kudziwa kwa kupambana kwa Mulungu
m' nkope ya Yesu Kristu.
7 Koma tiri ndi kulemera kumene m' dziwira dzadote, kuti
ukuru wambiri wa mpamvu ungokala ndi Mulungu, ndimo
8 si kwa ife toka; tititimizanidwa pa makundu onse, koma
sitisaukiridwa; tiganizidwaganizidwa, koma si kwa kuli-
9 zinga; titamangitsidwa, koma sitisiidwa; tigwetsedwa, koma
10 sitimwazidwa; ntawi yonse kunyamula m' tupi kupa kwa
Yesu, kuti moyo onso wa Yesu ungosonyezedwa m' tupi
11 latu. Kuti ife tomwe tiri ndi moyo ntawi yonse tipere-
kedwa kwa imfa kwa Yesu, kuti moyo onso wa Yesu ungoso-
12 nyezedwa m' nyama yatu yantembo. Ndimo tshointsho
13 imfa itshita mwa ife, koma moyo mwa inu. Koma tiri
ndi nzimu umodzi wa mvanu, monga amene omwe ale-
mbedwa, Dinamvana, ndimo tshointsho dinalankula; ife enso
14 timvana, ndimo tshointsho onso tilankula; kudziwa kuti
iemwe naukitsa Mwini Yesu adzaukitsa ife enso ndi Yesu,
15 ndimo adzaperekeza ife ndi inu. Kuti zintu zonse *ziri* kwa
inu, kuti kufatsa, kupindulidwa mwa unyinji, kungotshurutsa
kuamika kwa kupambana kwa Mulungu.
16 Mwa kuti sitifoka; koma ngati untu watu wakunja uliku-
bvunda, kosuntira unzimu watu ukonzetsedwa masiku onse.
17 Kuti sautso yopepuka yatu, yomwe iri kwa kantawi, itshita
kwa ife kopambana ndi kopambanitsa kulemera kosama-
18 riza kwa kupambana; ntawi sitiyang'ana pa zintu zomwe
ziri zoonedwa, koma pa zintu zomwe ziri zosaonedwa: kuti

zintu zomwe ziri zoonedwa ziri zantawi; koma zintu zomwe ziri zosaonedwa ziri zosamariza.

Kuti tidziwa kuti ngati nyumba yapansi ya msasa watu 5
isungunukidwa, tiri ndi kumanga kwa Mulungu, nyumba
yosamangidwa ndi manja, yosamariza, m' miamba. Kuti 2
nditu m' imene tibulira, kufuna kwambiri ku bvekedwa ndi
malo atu omwe ali kwa kumwamba: ngati kuli tshointsho 3
kuti kuli kubvekedwa sitidzapezedwa omariseke. Kuti 4
nditu ife tomwe tiri m' msasa umene tibulira, kulemedwa;
si kuti tifuna kusabvekedwa, koma kuti tifuna ku bvekedwa,
kuti tshomwe tshiri tshantembo tshingomezedwa ndi moyo.
Ndimo iemwe anatshita mwa ife kwa tshintu tshimenetshi 5
nditu ali Mulungu, emwe anapatsa kwa ife tshigwiriro tsha
Nzimu. Ndimo ntawi yonse tiri ndi kulimba ntima, ndimo 6
kudziwa kuti, ntawi tiri komwe m' tupi, tiribe kwa Mwini
(kuti tienda ndi mvanu, si ndi kuona); tiri olimba ntima, 7, 8
diti, ndimo tifuna kopambana ku li kutali ndi tupi, ndi ku
kala komwe ndi Mwini. Mwa kuti inso tipanga kutanda 9
kwatu, kapena komwe kapena kutali, ku kala osekera kwa
ie. Kuti ife tonse tikanasonyezedwa patsogolo pa mpando wa 10
kuweruza wa Kristu; kuti onse angolandira zintu *zitshitidwa*
mwa tupi, kwa komwe anatshita, kapena *kuli* bwino kapena
koipa.

Ndimo kudziwa kuopa kwa Mwini, tikantshizira antu, 11
koma tisonyezedwa kwa Mulungu; ndimo dilingalira kuti
tisonyezedwa anso m' madzidziwitso anu. Sitirikubvomereza 12
anso ife toka kwa inu, koma *tinena* monga kupatsa inu
tshifukwa tsha kupambana kwa ife, kuti mungokala ndi
kantu ku yang'ka awo omwe apambana m' kuona, ndi si m'
ntima. Kuti kapena tiri amisala, kuli kwa Mulungu; 13
kapena ngati tidziweruza, kuli kwa inu. Kuti kukonda kwa 14
Kristu kufulumiza ife; tshifuka tiweruza tshointsho, kuti
modzi anafera kwa onse, ndimo onse anafa; ndimo anafera 15
kwa onse, kuti awo omwe ali ndi moyo sakakala ndi moyo
onso kwa awo oka, koma kwa ie emwe anafera kwa awo
nauka anso. Ndimo ife kwa ntawi imene sitidziwa muntu 16
pambuiu pa nyama: inde ngati tinadziwa Kristu pambuiu
pa nyama, kosuntira tsopano ife tidziwa *ie tshointsho* si ntawi
ina. Mwa kuti ngati muntu modzi ali m' Kristu, *ali* 17
wopangidwa watsopano: zintu zakali zinapita; ona, zikala
zatsopano. Koma zintu zonse ziri za Mulungu, emwe 18
anayanja ife kwa ie eka mwa Kristu, natipatsa kuimirira

19 kwa kuanja; monga kuti Mulungu anali m' Kristu kuanja-
nitsa dziko kwa ie eka, sikuwereng'jera kwa awo matshimo
ao, ndimo anaika mwa ife mau a kuanja.
20 Ndimo tiri mitenga kwa Kristu, monga ngati Mulungu
alikupempa ndi ife: tipempa *inu* kwa Kristu, kalani oanjan-
21 idwa kwa Mulungu. Iemwe sanadziwa mpulupulu anapanga
*ku kala* mpulupulu kwa ife; kuti tinangokala kudeka kwa
6 Mulungu mwa ie. Ndimo kutshita *ndi ie* tipempa anso
2 kuti simulandira kufatsa kwa Mulungu mwa tshabe (kuti
anena,

Pa ntawi yolandiridwa dinamva ndi iwe,
Ndimo m' siku la kupulumutsa dinatangata iwe:

ona, tsopano iri ntawi yolandiridwa; ona, tsopano liri siku la
3 kupulumutsa): kupatsa palibe tshopuntwitsa m' kantu, kuti
4 kuimirira kwatu kusatshimikizidwa; koma m' zintu zonse
kudzibvomereza, monga oimirira a Mulungu, m' kulongosola
5 kwambiri, m' masautso, m' mafuno, m' zisoni, m' mikakato,
m' kuika m' nyumba za ndima, m' mapokoso, m' zintshito, m'
6 madikiro, m' kuleka kudia; m' kuyera, m' kudziwa, m'
kumva kutali, m' kukoma, m' Nzimu Woyera, m' kukonda
7 kosanyenga, m' mau a nteradi, m' mpamvu ya Mulungu;
m' ntshinjirizo wa kudeka pa dzanja lamanja ndi pa la-
8 manzere, ndi kupambana ndi kunyoza, ndi mbiri yoipa ndi
mbiri yabwino; monga onyenga, ndimo *kosuntira* anteradi;
9 monga osadziwidwa, ndi *kosuntira* odziwidwa bwino; monga
kufa, ndimo ona, tiri ndi moyo; monga kulangidwa, ndi
10 sikupedwa; monga atshisoni, kosuntira ntawi yonse kusekera;
monga osauka, kosuntira kupanga ambiri olemera; monga
kupotshera tshabe, ndimo *kosuntira* kukala ndi zintu
zonse.
11 Nkamwa mwatu mwatsegulidwa mwa inu, O Akorinte,
12 ntima watu ukulitsidwa. Musasaukitswa mwa ife, koma
13 musaukitswa m' makondo anu. Ndimo kwa sekeretso m'
mtundu umodzi (dinena monga kwa ana *anga*), mukulitsidwe
enso.
14 Musakomeredwa kosiana ndi osamvana: kuti kugawana
kwanje zipotshera kudeka ndi mpulupulu? kapena unzao
15 wanje kuunika kupotshera ndi ndima? Ndimo kuanja
kwanje Kristu apotshera ndi Beliyali? kapena kugawa
16 kwanje wamvanu apotshera ndi wosamvana? Ndimo
kugwirizana kwanje malo oyera a Mulungu apotshera
ndi mafano? Kuti ife tiri malo oyera a Mulungu wamo-

yo; inde monga Mulungu nanena, Didzakala mwa awo,
ndimo didzaenda mwa awo; ndimo didzakala Mulungu wao,
ndimo adzakala antu anga. Ndimo 17

Turukani mwa awo, ndimo ganikani,
ati Mwini,
Ndimo musatosa kantu kosatsuka;
Ndimo didzalandira inu,
Ndimo didzakala kwa inu Atate, 18
Ndimo mudzakala kwa ine ana amamuna ndi ana akazi,
ati Mwini Wampamvuyonse. Ndimo kuli ndi malonjezano 7
amene, okondedwa, tidzitsuke kwa kudetsa konse kwa nyama
ndi nzimu, kuta kuyera m' kuopa kwa Mulungu.

Tsegulani mitima yanu kwa ife: sitinatshimwitsa muntu, 2
sitinaipsa muntu, sitinatshenjerera muntu. Ditshinena siku- 3
sutsa *inu*: kuti danena patsogolo, kuti muli m' mitima yatu
ku fa pa modzi ndi ku kala ndi moyo pa modzi. Kwaku- 4
kuru kuli kulimbika kwanga kwa kunena kwa inu, kwaku-
kuru kuli kupambana kwanga kwa inu: didzazidwa ndi
kusangalatsa, disampuka ndi tshimwemwe m' sautso yatu
yonse.

Kuti inde ntawi tinafika m' Makedoniya, nyama yatu 5
inalibe kuleka, koma *ti*nasauts*wa* pa makundu onse; kunja
*anali* mamenyano, pakati *anali* maopa. Koma iemwe 6
asangalatsa osadzitama, *inde* Mulungu, nasangalatsa ife ndi
kufika kwa Tito; ndimo si ndi kufika kwatshi koka, koma 7
anso ndi kusangalatsa ndi komwe anasangalatsidwa mwa inu,
ntawi anauza ife kufuna kwanu, kulira kwanu, tshangu
tshanu kwa ine; monga kuti dinasekera inde kopambana.
Kuti ngati dinapanga inu atshisoni ndi epistola langa, 8
sindimva tshisoni ndi ilo, ngati dinamva tshisoni; kuti diona
kuti epistola lidya linapanga inu atshisoni, ngati koma kwa
nsiku. Tsopano disekera, si kuti munapangidwa atshisoni, 9
koma kuti munapangidwa atshisoni kwa kutembenuza
ntima: kuti munapangidwa atshisoni kwa Mulungu, kuti
munangomva kumwaza mwa ife m' tshabe. Kuti tshisoni 10
kwa Mulungu tshitshita kutembenuza ntima kwa kupulu-
mutsa, *kutembenuza ntima* komwe kusatenga tshisoni: koma
tshisoni tsha dziko tshitshita imfa. Kuti ona, tshintu 11
tshimenetshi, kuti munapangidwa atshisoni kwa Mulungu,
kusunga kolimba kwanje kunapanga mwa inu, inde,
kudzikana kwanje kwa inu noka, inde, kukwia kwanje, inde,

kuopa kwanje, inde, kufuna kwanje, inde, tshangu tshanje,
inde, kuzimbula kwanje! M' zintu zonse munadzisimba ku
12 kala oyera m' tshintu. Kuti ngati dinalemba kwa inu,
*dinalemba* si kwa tshifukwa tshatshi emwe anatshimwa,
kapena kwa tshifukwa tshatshi emwe anamva tshimo, koma
kuti kusunga kolimba kwanu kwa ife kunangosonye-
13 zedwa kwa inu m' kuona kwa Mulungu. Ndimo tasangala-
tsidwa: ndimo m' kusangalala kwatu tinasekera kwambiri
kopambana kwa tshimwemwe tsha Tito, tshifuka nzimu
14 watshi wadzisangalatsidwa ndi inu nonse. Kuti ngati mwa
kantu dinapambana ku ie kwa inu, sindinapatsidwa ma-
nyazi; koma monga tinalankula zintu zonse kwa inu m'
nteradi, tshointsho kupambana kwatu unso, komwe dina-
panga patsogolo pa Tito, kunapezedwa ku li nteradi.
15 Ndimo kukonda kwa ntima watshi kuli kutshuruka kopa-
mbana kwa inu, ntawi akumbukila kumvera kwa inu nonse,
bwanje ndi kuopa ndi kuntentemera munalandira ie.
16 Disekera kuti mwa zintu zonse diri ndi kulimbika ntima
kwa inu.
8 Koma, abali, tidziwitsa inu kufatsa kwa Mulungu komwe
2 kwapatsidwa m' maeklesia a Makedoniya; bwanje kuti m'
kuyesa kwambiri kwa sautso kutshuruka kwa tshimwemwe
tshao ndi kusauka kwambiri kwao kunatshuruka kwa
3 zolemera za kupatsa kwao. Kuti ndi mpamvu yao, dima-
riza, inde ndi kopambana mpamvu yao, *napatsa* ndi mitima
4 yao, kupempa ife ndi kupempa kwambiri ndi kufatsa
5 kumene ndi unzao m' kuimirira kwa oyera: ndi *tshimene*, si
monga tinalingalira, koma poiamba napatsa awa oka kwa
6 Mwini, ndi kwa ife ndi kufuna kwa Mulungu. Monga kuti
tinataulira Tito, kuti monga anapanga kuiamba patsogolo,
tshointsho akanata anso mwa inu kufatsa kumene enso.
7 Koma monga mutshurutsa mwa zintu zonse, *m'* mvanu, ndi
kunena, ndi kudziwa, ndi *m'* kulimbika konse, ndi *m'*
kukonda kwanu kwa ife, *ona* kuti mutshurutsa m' kufatsa
8 kumene enso. Sindinena monga mau, koma monga ku-
yesa mwa kulimbika kwa ena nteradi inso wa kukonda
9 kwanu. Kuti mudziwa kufatsa kwa Mwini watu Yesu
Kristu, kuti, ngati anali wolemera, koma kwa inu nakala wo-
sauka, kuti inu mwa kusauka kwatshi munangokala olemera.
10 Ndimo m' tshimene dipatsa kuweruza *kwanga:* kuti tshi-
mene tshiri tshabwino kwa inu, omwe anali oiamba ku
panga kuiamba tshaka tshinapita, si ku tshita koka, koma

anso ku funa. Koma tsopano itani kutshita anso; kuti 11
monga *kunali* kuta ku funa, tshointsho *kungokala* kumariza
anso mwa mpamvu yanu. Kuti ngati kuta kulipo, *kuli* 12
kolandiridwa monga *muntu* apotshera, si monga wosapo-
tshera. Kuti *sindinena tshimene*, kuti ena angopeputsidwa, 13
*ndi* inu mungolemedwa: koma ndi umodzi; kutshuruka 14
kwanu *kukala kukwanitsa* pa ntawi yatsopano imene kwa
kufuna kwao, kuti kutshuruka kwao onso kungokala
*kukwanitsa* kwa kufuna kwanu; kuti kungokala umodzi:
monga alembedwa, Iemwe *anasong'ketsa* kwambiri sanapo- 15
tshera kantu kotsala; ndimo iemwe *anasong'ketsa* kang'ono
sanapotshera kupanda.

Koma tshakoma kwa Mulungu, emwe aika kusunga 16
kolimba kumene kwa inu muntima wa Tito. Kuti nditu 17
nalandira kutaulira kwatu; koma ali ie eka wolimbika
nditu, naturuka kwa inu ndi ntima watshi. Ndimo tatumiza 18
ndi ie mbali wa emwe kutama kwatshi m' ivangeli *kubu-
kitswa* m' maeklesia onse; ndimo si tshointsho oka, koma 19
emwe analoezedwa anso ndi maeklesia ku enda ndi ife m'
*tshifukwa tsha* kufatsa kumene, komwe kuimiriridwa ndi
ife kwa kupambana kwa Mwini, ndimo *ku sonyeza* kuta
kwatu: kulambalala kumene, kani muntu modzi akatshula 20
ife m' *tshifukwa tsha* kwanja kumene, komwe kuimiriridwa
ndi ife: kuti tiganiza ndi zintu zaulemu, si koka m' kuona 21
kwa Mwini, koma anso m' kuona kwa antu. Ndimo 22
tatumiza ndi awo mbali watu, emwe tayesa wolimbika
ntawi zambiri m' zintu zambiri, koma tsopano wolimbika
kwambiri kopambana, ndi tshifukwa tsha mvanu woukuru
womwe *wapotshera* mwa inu. Kapena ngati *wina afunsira* 23
ndi Tito, *ali* wogawana wanga ndi wotshita nza*nga* kwa inu;
kapena abali atu, *ali* mitenga ya maeklesia, *ali* kupambana
kwa Kristu. Ndimo sonyezani kwa awo m' nkope ya 24
maeklesia kumariza kwa kukonda kwanu, ndi kwa kupa-
mbana kwatu kwa inu.

Kuti monga ndi kuimirira kwa oyera, kuli kopambana 9
kwa ine ku lemba kwa inu: kuti didziwa kuta kwanu, ndi 2
komwe dipambana kwa inu ku awo a Makedoniya, kuti
Akaya wafotokozedwa kwa tshaka tshapita; ndi tshangu
tshanu tshafulumiza unyinji wa awo. Koma datumiza 3
abali, kuti kupambana kwatu kwa inu kusangopangidwa
tshabe m' tshimene; kuti, inde monga dinanena, mungofo-
tokozedwa: kani ndi kantu, ngati afika ndi ine ena a 4

Makedoniya, napeza inu osata, ife (kuti sitinena, inu)
5 tikanapatsidwa manyazi m' kumvana kumene. Ndimo
dinatshiganiza uko ku pempa abali, kuti akapita patsogolo
kwa inu, ku dzazitsa patsogolo kwanja kwanu kwalonjeze-
dwa kali, kuti komwe kudzata, monga tshintu tsha kwanja,
ndimo si tsha kuawanya.
6 Koma tshimene *dinena*, Iemwe afesa kotalikitsa adzatema
anso kotalikitsa; ndi iemwe afesa kotshurukitsa adzatema
7 anso kotshurukitsa. Antu onse *atshite* monga anayerekeza
m' mitima yao; si kouma ntima, kapena ndi uko: kuti
8 Mulungu akonda wopatsa wosekera. Ndimo Mulungu ali
ndi mpamvu ku panga kufatsa konse ku tshurutsa kwa inu;
kuti inu, kupotshera ntawi yonse kutshuruka konse m' zintu
9 zonse, mungotshurutsa kwa ntshito zonse zabwino: monga
alembedwa,

Wabalalitsa, wapatsa kwa osauka;
Kudeka kwatshi kukala kwa ntawi yonse.

10 Ndimo emwe akwanitsa mbeu kwa wofesa ndi nkate kwa
kudia, adzakwanitsa ndimo adzapindula mbeu yanu kwa
kufesa, ndimo adzakulitsa dzobala dza kudeka kwanu:
11 mulemezedwa m' zintu zonse kwa kupatsa konse, komwe
12 kutshita mwa ife kunena tshakoma kwa Mulungu. Kuti
kuimirira kwa ntshito imene sikudzaza koka muyezo wa
zofuna za oyera, koma kutshurukitsa anso mwa kunena
13 tshakoma kwambiri kwa Mulungu; kuona kuti mwa kuyesa
*kwa inu* ndi kuimirira kumene apambanitsa Mulungu kwa
kumvera kwa kubvomereza kwanu kwa ivangeli wa Kristu,
ndi kwa kupatsa kwa song'kanitso *lanu* kwa awo ndi kwa
14 onse; ntawi awo oka anso, ndi kupempera kwa inu, afuna
inu kwambiri tshifuka tsha kufatsa kutshuruka kwa Mulungu
15 mwa inu. Tshakoma kwa Mulungu kwa tshaulere tshatshi
tshosaneneka.

10 Ndimo ine ndeka Paulos, dipempa inu ndi kuanja ndi
ulere za Kristu, ine emwe m' kuona kwanu diri kofatsa
2 mwa inu, koma diribe diri ndi kulimba ntima kwa inu: inde,
dipempa inu, kuti ntawi diri ndi inu sindingosonyeza kuli-
mbika ntima ndi kumvana ndi womwe diwerenga ku kala
kolimba pa ena, omwe awerenga ndi ife monga ngati tina-
3 endaenda kwa nyama. Kuti ngati tienda m' nyama, sitipa-
4 nga nkondo monga kwa nyama (kuti mauta a nkondo yatu
osali a nyama, koma olimba patsogolo pa Mulungu kwa
5 kuponya pansi a malinga); kuponya pansi maganizo, ndi

zintu zonse zazitali zomwe zitalitsidwa pa kudziwa kwa
Mulungu, ndimo ku tenga ntintu zonse mwa umpawi kwa
kumvera kwa Kristu; ndimo tiri kuta ku zimbula kusa- 6
mvera konse, ntawi kumvera kwanu kudzadzazidwa. Mu- 7
yang'anira pa zintu zomwe ziri patsogolo nkope yanu. Ngati
muntu modzi amvana ndi ie eka kuti ali wa Kristu, aganize
tshimene enso ndi ie eka, kuti, inde monga ali wa Kristu,
tshointsho onso tiri. Kuti ngati dikapambana kantu kaku- 8
kuru ndi kuweruza kwatu (komwe Mwini anapatsa kwa
kumanga inu, ndimo si kwa kuponya inu pansi), sindidzapatsi-
dwa manyazi: kuti sindingoenedwa monga ngati dikaopetsa 9
inu ndi maepistola anga. Kuti, Maepistola atshi, ati, ali 10
olemera ndi olimba; koma makalidwe a tupi latshi ali ofoka,
ndi kunena kwatshi kuli tshabe. Modzi wotere awerenge 11
tshimene, kuti, tshomwe tiri m' mau ndi maepistola ntawi
tiribe, otere enso *tiri* nditu ntawi tiripo. Kuti sitiri olimba 12
ku werenga kapena ku fanizira ife toka ndi ena a awo omwe
adzibvomereza: koma iwo oka, kulinganiza iwo oka ndi iwo
oka, ndi kufanizira iwo oka ndi iwo oka, ali opanda ku-
dziwitsa. Koma sitidzapambana kopambana kulinganiza 13
*kwatu*, koma kwa kulinganiza kwa mulinganizo womwe
Mulungu anagawa kwa ife monga mulinganizo, ku fika inde
kwa inu. Kuti sititamula ife toka tshuruka kopambana, 14
monga ngati sitinafika kwa inu: kuti tinafika inde monga
kutali monga kwa inu m' ivangeli wa Kristu: sikupambana 15
kopambana kulinganiza *kwatu*, *tshomwe tshiri*, m' ntshito za
antu ena; koma ku potshera kulingalira kuti, monga
mvanu wanu ukula, tidzakulitsidwa mwa inu kwa mulinga-
nizo watu kwa kutshuruka *kopambana*, tshointsho monga 16
ku uza ivangeli inde kwa patsidia pa inu, *ndimo* siku-
pambana m' mulinganizo wa wina ndi zintu zonse zirikuta
kwa dzanja latu. Koma iemwe apambana, apambane m' 17
Mwini. Kuti si ie emwe adzibvomereza asimbidwa, koma 18
emwe Mwini abvomereza.

Difuna kuti mulikumva ndi ine ndi kupusa kwakung'ono: 11
koma nditu mumva ndi ine. Kuti diri wansanje pa inu ndi 2
nsanje ya Mulungu: kuti dinakwatitsa inu kwa mamuna
modzi, kuti dinangopereka inu *monga* tshiweta tshoyera kwa
Kristu. Koma diopa, kani ndi zifukwa zina, monga njoka 3
inanyenga Heva m' tshinyengo tsha iyo, ntintu zanu zikana-
bvunditsidwa kwa umodzi ndi kuyera zomwe ziri ku Kristu.
Kuti ngati iemwe afika auza Yesu wina, emwe sitinauza, 4

kapena *ngati* mulandira nzimu wa mtundu wina, womwe
musanalandira, kapena ivangeli wa mtundu wina, womwe
5 musanalandira, mutshita bwino ku mva ndi *ie*. Kuti di-
werenga kuti sindiri kakang'ono pambuiu apostile akuru
6 opambana nditu. Koma ngati *diri* wotsiruka m' kunena, ko-
ma s*indiri wotsiruka* m' kudziwa; iai, m' zintu zonse tina*tshi*-
7 sonyeza mwa antu onse kwa inu. Kapena kodi dinatshita
tshimo m' kutshepetsa ine ndeka kuti munangopambanitswa,
tshifuka dinauza kwa inu ivangeli wa Mulungu kwa tshabe?
8 Dinalanda maeklesia ena, kulandira kulipira *kwa awo* kuti
9 dinangoimirira kwa inu; ndimo ntawi dinali ndi inu ndimo
dinali m' kusauka, sindinali katundu pa muntu modzi; kuti
abali, ntawi anafika kwa Makedoniya, anakwanitsa tshomwe
tshiri tshopanda kwa ine; ndimo m' zintu zonse dinasunga
ine ndeka kuti sindikala katundu kwa inu, ndimo *tshointsho*
10 didzasunga *ine ndeka*. Monga nteradi wa Kristu uli mwa
ine, palibe muntu adzaletsa ine kwa kupambana kumene m'
11 maiko a Akaya. Mwa kuti? tshifuka sindikonda inu?
12 Mulungu adziwa. Koma tshomwe ditshita, tshimene didza-
tshita, kuti didzatshotsa tshifukwa kwa awo omwe afuna
tshifukwa; kuti momwe apambana, angopezedwa inde
13 monga ife. Kuti antu otere ali apostile onyenga, otshita
14 onyenga, kudzifaniza m' apostile a Kristu. Ndimo palibe
kuzizwa; kuti inde Satana adzifaniza m' njelo wa kuunika.
15 Ndimo sitshiri tshintu tshatshikuru ngati oimirira atshi inso
adzifaniza monga oimirira a kudeka; nsonga ya omwe
idzakala kwa ntshito zao.
16 Dinena anso, Palibe muntu modzi aganize ine wopusa;
koma ngati *mutshita*, kosuntira monga wopusa landirani ine,
17 kuti ine enso dingopambana kang'ono. Tshimene tshomwe
dilankula, dilankula si pambuiu Mwini, koma monga
18 m' kupusa, m' kumvana kumene kwa kupambana. Kuona
kuti ambiri apambana pambuiu nyama, didzapambana anso.
19 Kuti mumva ndi opusa kosekera, muli anzeru *inu noka*.
20 Kuti mumva ndi muntu, ngati atenga inu mwa umpawi,
ngati ameza inu, ngati agwira inu *mikoli*, ngati adzitali-
21 kitsa, ngati amenya inu pa nkope. Dinena ndi kutshepetsa,
monga ngati tinali ofoka. Koma m' tshimene tshomwe
modzi ali wolimba (dinena m' kupusa), diri wolimba anso.
22 Kodi ali Ahebere? tshointsho ndiri. Kodi ali Asirayeli?
tshointsho ndiri. Kodi ali mbeu ya Abraham? tshointshi
23 ndiri. Kodi ali oimirira a Kristu? (dilankula monga modzi

wamisala) ine wopambana; m' zintshito kutshuruka kopa-
mbana, m' nyumba za ndima kutshuruka kopambana,
m' mikakato yopambana kulinganiza, m' ziimfa ntawi
zambiri. Kwa Ayuda dinalandira ntawi zisanu *mikakato* 24
makumi anai wotsala umodzi. Ntawi zitatu dinamenyedwa 25
ndi zintole, ntawi imodzi dinaponyedwa miala, ntawi zitatu
dinabandulidwa m' tshombo, usiku ndi msana dali m' kuya;
*m'* maulendo ntawi zambiri, *m'* mapanikizo a mitsinje, 26
*m'* mapanikizo a olanda, *m'* mapanikizo kwa fuko *langa*,
*m'* mapanikizo kwa Mitundu, *m'* mapanikizo muzinda,
*m'* mapanikizo m' tshipululu, *m'* mapanikizo m' nyanja,
*m'* mapanikizo mwa abali onyenga; *m'* kulema ndi kutshita, 27
m' madikiro ntawi zambiri, m' njala ndi ludzu, m' kuleka
kudia ntawi zambiri, m' kuzizira ndi mwa usiwa. Kopa- 28
mbana zintu zidya zomwe ziri zakunja, tshiri tshomwe
tshisindikiza pa ine masiku onse, kufunsafunsa kwa ma-
eklesia onse. Ndani ali wofoka, ndimo sindiri wofoka? 29
ndani akwiitsidwa, ndimo sindiotsha? Ngati dikanapa- 30
mbana, didzapambana ndi zintu zomwe zikala ndi kufoka
kwanga. Mulungu ndi Atate a Mwini Yesu, iemwe ali 31
wodala kwa magonero, adziwa kuti sindinama. M' Damasko 32
mbiri pansi pa Areta fumu yotshuka analikudikira mzinda
wa Adamasko, ku gwira ine: ndi mwa zanera dinasitswa 33
mutanga pa koma, napulumuka manja atshi.

Dikanapambana, ngati tshosali tshapindulidwa; koma 12
didzafika kwa zoona ndi masonyezo za Mwini. Didziwa 2
muntu m' Kristu, dzaka kumi ndi dzinai dzinapita (kapena
m' tupi, sindidziwa; kapena kunja kwa tupi, sindidziwa;
Mulungu adziwa), modzi wotere natukulidwa inde kwa
mwamba mwatshitatu. Ndimo didziwa muntu wotere 3
(kapena m' tupi, kapena wobaluka kwa tupi, sindidziwa;
Mulungu adziwa), bwanje kuti natukulidwa m' Paradisi, 4
ndi namva mau osaneneka, omwe osali amau kwa muntu
ku lankula. Kwa modzi wotere didzapambana: koma 5
kwa ine ndeka sindidzapambana, koma m' mafoko *anga*.
Kuti ngati dikafuna ku pambana, sindidzakala wopusa; 6
kuti didzanena nteradi: koma dileka, kani muntu modzi
akawerenga ndi ine kopambana kumene komwe aona ine
*ku kala* kapena amva kwa ine. Ndimo ndi tshifukwa tsha 7
ukuru wopambana wa masonyezo—ndimo, kuti sindikataliki-
tsidwa kotshuruka kopambana, unapatsidwa kwa ine munga
m' nyama, mtenga wa Satana ku tundudza ine, kuti sindi-

8 katalikitsidwa kotshuruka kopambana. Ndi tshintu tshi-
mene dinapempa Mwini katatu, kuti tshinangotshoka kwa
9 ine. Ndimo wanena ndi ine, Kufatsa kwanga kuli ku-
tshuruka kwa iwe: kuti mpamvu *yanga* ipangidwa yakuta
m' kufoka. Ndimo kosekera nditu didzapambana kopa-
mbana m' mafoko anga, kuti kulimba kwa Kristu kungokala
10 pa ine. Mwa kuti disekera m' mafoko, m' mapweteko,
m' mauko, m' mazunzo, m' zisoni, kwa Kristu: kuti ntawi
diri wofoka, pomwe diri wolimba.
11 Dikala wopusa: munafulumiza ine; kuti dikanabvomere-
zedwa ndi inu: kuti m' palibe kantu dinali pambuiu apostile
12 akuru nditu, ngati diri tshabe. Nditu zizindikilo za mpostile
zinatshitidwa mwa inu m' kulongosola konse, ndi zizindikilo
13 ndi zozizwa ndi zimpamvu. Kuti tshiri tshiani mwa kuti
munapangidwa ang'ono ndi maeklesia ena, kani *kuli* kuti
ine ndeka sindinali katundu kwa inu? kululukirani ine
tshimo limene.
14 Ona, imene iri ntawi yatshitatu diri kuta ku fika kwa
inu; ndimo sindidzakala katundu kwa inu: kuti sindifuna
zanu, koma inu: kuti ana sakanaika kwa atatu ao ndi amai
15 ao, koma atatu ndi amai kwa ana. Ndimo kosekera nditu
didzatshita ndimo didzatshitidwa kwa mizimu yanu. Ngati
dikonda inu kotshuruka kopambana, kodi dikondedwa
16 kwakung'ono kopambana? Koma tshikale tshointsho, sindi-
napatikiza inu ine ndeka; koma, dinali wotshenjera, dina-
17 gwira inu ndi tshinyengo. Kodi dinatshenjerera inu ndi
18 modzi wa awo omwe datumiza kwa inu? Dinataulira Tito,
ndimo dinatumiza mbali nai'. Kodi Tito anatshenjerera
inu? kodi sitinaendaenda ndi Nzimu umodzi? kodi si*ti-
naendaenda* m' mapazi amodzi?
19 Muganiza ntawi yonse imene tirikudzipambanuza kwa inu.
M' kuona kwa Mulungu tilankula m' Kristu. Koma zintu
20 zonse, okondedwa, *ziri* kwa kumanga kwanu. Kuti diopa,
kani ndi zifukwa zina, ntawi difika, dikapeza inu si otere
monga difuna, ndimo ine ndeka dikapezedwa ndi inu wotere
monga musafuna; kani ndi zifukwa zina *zikakala* ndeu,
nsanje, makwiiro, magawano, miseke, manong'ono, maku-
21 litso, mapokoso; kani, ntawi difika anso, Mulungu wanga
akatshepetsa ine patsogolo pa inu, ndimo dikalira kwa
ambiri a awo omwe anatshimwa patsogolo, ndimo sanate-
mbenuza mitima yao kwa kusatsuka ndi dama ndi mafuno
a tshigololo zomwe anatshita.

Imene iri ntawi yatshitatu dirikufika kwa inu. Pa nka- 13
mwa mwa omariza awiri kapena atatu mau onse adzalimbitsi-
dwa. Dati kali, ndimo dinena kali, monga ntawi dinalipo 2
ntawi yatshiwiri, tshointshi tsopano, diribe, ku awo omwe
anatshimwa ntawi yapita, ndi kwa onse ena, kuti, ngati
didza anso, sindidzayanja; kuona kuti mufuna kumariza 3
kwa Kristu emwe alankula mwa ine; emwe kwa inu wosali
wofoka, koma ali ndi mpamvu mwa inu: kuti anapatshi- 4
kidwa mwa kufoka, koma akala ndi moyo mwa mpamvu ya
Mulungu. Kuti ife enso tiri ofoka mwa ie, koma tidzakala
ndi moyo ndi ie mwa mpamvu ya Mulungu kwa inu.
Yesani inu noka, ngati mukala ndi mvanu; funsirani inu 5
noka. Kapena kodi simudziwa monga kwa inu noka, kuti
Yesu Kristu ali mwa inu? kani nditu muli otaiidwa. Koma 6
dilingalira kuti mudzadziwa kuti sitiri otaiidwa. Ndimo 7
tipempera Mulungu kuti musatshita mpulupulu; si kuti
tingosonyezedwa osimbidwa, koma kuti mungotshita tshi-
mene tshomwe tshiri tshaulemu, ngati tikala monga otai-
idwa. Kuti sitidziwa ku tshita kantu pa nteradi, koma kwa 8
nteradi. Kuti tisekera, ntawi tiri ofoka, ndimo muli 9
olimba: tshimene tipempera anso, inde kuta kwanu. Kwa 10
tshifukwa tshimene dilemba zintu zimenezi ntawi diribe, kuti
sindingotshita kolimbika ntawi diripo, kwa kuweruza komwe
Mwini anapatsa ine kwa kumanga, ndimo si kwa kuponya
pansi.

Kwakutungo, abali, kalani bwino. Mutedwe; musanga- 11
latsidwe; kalani ndi muwongo umodzi; kalani ndi ntendere:
ndi Mulungu wa kukonda ndi ntendere adzakala ndi inu.
Utsanani ndi kumsomsona koyera. 12

Oyera onse autsa inu. 13

Kufatsa kwa Mwini Yesu Kristu, ndi kukonda kwa 14
Mulungu, ndi unzatshi wa Nzimu Woyera, zikale ndi inu
nonse.

EPISTOLA LA PAULOS KWA

# AGALATIYA.

PAULOS, mpostile (si kwa antu, kapena mwa muntu,
2 koma mwa Yesu Kristu, ndi Mulungu Atate, emwe
3 anaukitsa ie kwa akufa), ndi abali onse omwe ali ndi ine,
4 kwa maeklesia a Galatiya: Kufatsa kwa inu ndi ntendere
kwa Mulungu Atate, ndi Mwini watu Yesu Kristu, emwe
anapatsa ie eka kwa mpulupulu zatu, kuti anangopulumutsa
ife mwa kugonera kumene koipa kwatsopano, kwa kufuna
5 kwa Mulungu watu ndi Atate: kwa emwe *kuli* kupambana
kwa magonero a magonero. Amen.
6 Dizizwa kuti mulikusuntira nsanga kotere kwa ie emwe
anaitana inu m' kufatsa kwa Kristu kwa ivangeli wina;
7 womwe wosali *ivangeli* wina: koma alipo ena omwe abvuta
8 inu, nafuna ku kotetsa ivangeli wa Kristu. Koma ngati ife,
kapena njelo kwa kumwamba, akauza kwa inu ivangeli
umodzi, wina ndi uo womwe tinauza kwa inu, ie atukwa-
9 nidwe. Monga tanena patsogolo, tshointsho dinena tsopano
onso, Ngati muntu modzi auza kwa inu ivangeli umodzi,
10 wina ndi uo womwe munalandira, ie atukwanidwe. Kuti
kodi tsopano dirikukantshizira antu, kapena Mulungu?
kapena kodi dirikufuna ku sekeretsa antu? ngati kosuntira
dinalikusekeretsa antu, sindikakala kapolo wa Kristu.
11 Kuti didziwitsa inu, abali, monga ndi ivangeli womwe
12 unauzidwa ndi ine, kuti wosali pambuiu muntu. Kuti
kapena sindinaulandira kwa muntu, kapena sindinaupunzi-
tsidwa, koma *unafika kwa ine* mwa kusonyeza kwa Yesu Kristu.
13 Kuti munamva ndi makalidwe a moyo wanga mu ntawi
yapita m' kupembedza kwa Ayuda, bwanje kuti kopambana
kulinganiza dinazunza eklesia la Mulungu, ndinamwaza
14 ilo: ndimo dinaposa m' kupembedza kwa Ayuda patsogolo
ambiri a anzanga mwa fuko langa, dinali watshitsanzo kopa-
15 mbana kwa miambi ya atatu anga. Koma ntawi kunali
kusekera kwabwino kwa Mulungu, emwe analekanitsa ine,
*inde* kwa tshibaliro tsha amai anga, ndimo naitana ine mwa

kufatsa kwatshi, ku sonyeza Mwana watshi mwa ine, kuti 16
dinangouza ie mwa Mitundu; tsopano lino sindinaganiza ndi
nyama ndi mwazi: kapena sindinakwera ku Yerusalem kwa 17
omwe anali apostile patsogolo pa ine: koma damuka mwa
Arabe; ndimo onso dinabwera ku Damasko.

Ndimo pambuiu dzaka dzitatu dinakwera ku Yerusalem 18
ku tsheza ndi Kefa, nakala nai' masiku kumi ndi asanu.
Koma ena a apostile sindinaona palibe, koma Yakobi 19
mpwatshi wa Mwini. Ndimo ndi zintu zomwe dilemba kwa 20
inu, ona, patsogolo pa Mulungu, sindinama. Pomwe dinafika 21
m' maiko a Siriya ndi Kilikiya. Ndimo kosuntira sindina- 22
dziwidwa ndi nkope kwa maeklesia a Yudeya omwe anali
m' Kristu: koma koka anamva kuti, Iemwe kali anazunza 23
ife tsopano auza mvanu wa womwe kali namwaza; ndimo 24
napambanitsa Mulungu mwa ine.

Ndimo pambuiu ntawi ya dzaka kumi ndi dzinai dinakwera 2
anso ku Yerusalem ndi Barnaba, kutenga Tito onso ndi ine.
Ndimo dinakwera ndi kusonyeza; ndimo dinaika patsogolo pa 2
awo ivangeli womwe diuza mwa Mitundu, koma kutseri
patsogolo pa awo omwe anali ndi mbiri, kani ndi kantu
dikalikutamanga, kapena dinatamanga, kwa tshabe. Koma 3
si inde Tito emwe anali ndi ine, anali Mgrike, anafulumizi-
dwa ku dulidwa: ndi tshimene tshifuka tsha abali onyenga 4
kutseri analoezedwa, omwe analoa kutseri ku zonda ufulu
watu womwe tipotshera m' Kristu Yesu, kuti anangotenga
ife m' umpawi: kwa omwe tinapatsa malo ndi kukala pansi, 5
iai, si kwa ora limodzi; kuti nteradi wa ivangeli unangokalabe
ndi inu. Koma kwa adya omwe anabukitsidwa ku li kantu 6
(kantu komwe anali, tshiri tshabe kwa ine: Mulungu wosa-
landira makalidwe a muntu)—awo omwe anali ndi mbiri
sanapatsa kantu kwa ine: koma kodulitsa, ntawi anaona 7
kuti dinamvanidwa ndi ivangeli wa kusadula, inde monga
Petros ndi *ivangeli* wa kudula (kuti iemwe anatshita kwa 8
Petros kwa upostile kwa kudula anatshita kwa ine enso kwa
Mitundu); ndimo ntawi nadziwitsa kufatsa komwe kunapa- 9
tsidwa kwa ine, Yakobi ndi Kefa ndi Yohane, awo omwe
anabukitsidwa ali mizati, napatsa kwa ine ndi Barnaba manja
akudiera a unzao, kuti tikaenda kwa Mitundu, ndimo awo
kwa kudula; koka *nafuna* kuti tikakumbukila osauka; 10
tshintu tshimene nditu dinali watshitsanzo onso ku tshita.

Koma ntawi Kefa nafika ku Antiyokwe, dinakaniza ie kwa 11
nkope, tshifuka naima wosutsidwa. Kuti patsogolo kuti ena 12

nadza kwa Yakobi, nadia ndi Mitundu: koma ntawi anafika,
nadzibweza nadzilekanitsa, kuopa awo omwe anali a kudula.
13 Ndimo otsala a Ayuda anama anso nai'; monga ambiri
14 kuti inde Barnaba anyamulidwa ndi kunama kwao. Koma
ntawi dinaona kuti sanaenda kodeka kwa nteradi wa
ivangeli, dinanena ndi Kefa patsogolo pa *awo* onse, Ngati
iwe, uli Myuda, ukala ndi moyo monga ikala Mitundu,
ndimo si monga akala Ayuda, bwanje ufulumiza Mitundu
15 ku kala ndi moyo monga akala Ayuda? Ife tiri Ayuda ndi
16 makalidwe, ndimo si ampulupulu a Mitundu, koma kudziwa
kuti muntu wosadeketsedwa ndi ntshito za mau, koma koka
mwa mvanu m' Yesu Kristu, inde tinamvana pa Kristu
Yesu, kuti tinangodeketsedwa ndi mvanu m' Kristu, ndimo
si ndi ntshito za mau: tshifuka ndi ntshito za mau palibe
17 nyama idzadeketsedwa. Koma ngati, ntawi tinafuna ku
deketsedwa m' Kristu, ife toka anso tinapezedwa ampulupulu,
kodi Kristu ali woimirira wa mpulupulu? Si tshointsho.
18 Kuti ngati dimanga anso zintu zimenezo zomwe dinamwaza,
19 didzisonyeza wotshimwa. Kuti ine mwa mau dinafa kwa
20 mau, kuti dinangokala ndi moyo kwa Mulungu. Dapatshi-
kidwa ndi Kristu; koma dikala ndi moyo; *koma* si ntawi
ina ine, koma Kristu akala ndi moyo mwa ine: ndimo *moyo*
umene womwe tsopano dikala ndi moyo m' nyama dikala ndi
moyo m' mvanu, *mvanu* womwe uli m' Mwana wa Mulungu,
21 emwe nakonda ine, nadzipereka kwa ine. Sindipanga
tshabe kufatsa kwa Mulungu: kuti ngati kudeka kuli mwa
mau, pomwe Kristu nafera kwa tshabe.

3 O Agalatiya opusa, ndani analodza inu, patsogolo pa maso
a omwe Yesu Kristu anaikidwa poyera wopatshikidwa?
2 Tshimene tshoka difuna ku punzira kwa inu, Kodi munala-
ndira Nzimu ndi ntshito za mau, kapena ndi kumva kwa
3 mvanu? Kodi muli opusa otere? kunaamba m' Nzimu,
4 kodi mulikutedwa tsopano m' nyama? Kodi munamva
zintu zambiri zotere kwa tshabe? ngati nditu kuli kwa
5 tshabe. Ndimo iemwe akwanitsa kwa inu Nzimu, natshita
zimpamvu mwa inu, kodi *akutshita* ndi ntshito za mau,
6 kapena ndi kumva kwa mvanu? Inde monga Abraham
namvana ndi Mulungu, ndimo unawereng'jedwa kwa ie kwa
7 kudeka. Ndimo dziwani kuti awo omwe ali ndi mvanu,
8 amene ali ana a Abraham. Ndimo lemba, kuona patsogolo
kuti Mulungu akadeketsa Mitundu ndi mvanu, linauza
ivangeli patsogolo kwa Abraham, *kuti*, Mwa iwe mitundu

yonse idzadalitsidwa. Ndimo tshointsho awo omwe ali a 9
mvanu adalitsidwa ndi Abraham wamvanu. Kuti monga 10
ambiri monga ali a ntshito za mau ali pansi pa tukwano:
kuti alembedwa, Otukwanidwa ali onse omwe osakalabe m'
zintu zonse zomwe zilembedwa m' buku la mau, ku tshita
izo. Ndimo kuti palibe muntu adeketsedwa ndi mau m' 11
kuona kwa Mulungu, kuli kuenedwa: kuti, Wodeka adza-
kala ndi moyo ndi mvanu; ndimo mau osali a mvanu; koma, 12
Ie emwe atshita izo adzakala ndi moyo mwa izo. Kristu 13
anaombola ife kwa tukwano la mau, kunakala tukwano kwa
ife: kuti alembedwa, Otukwanidwa ali onse omwe apatshi-
kidwa pa ntengo: kuti pa Mitundu kunangofika kudala kwa 14
Abraham m' Kristu Yesu; kuti tinangolandira lonjezano la
Nzimu mwa mvanu.

Abali, dinena pambuiu pa makalidwe a antu: Ngati 15
kuli koma kupangana kwa muntu, kosuntira ntawi kwa-
limbitsidwa, palibe modzi akupanga tshabe, kapena aong'-
khetsa kwa iko. Koma kwa Abraham malonjezano 16
ananenedwa, ndi kwa mbeu yatshi. Wosanena, Ndi kwa
zimbeu, monga ndi zambiri; koma monga ndi imodzi, Ndi
kwa mbeu yako, yomwe iri Kristu. Koma dinena tshimene; 17
Kupangana kulimbikitsidwa patsogolo ndi Mulungu, mau,
omwe anafika dzaka mazana anai ndi makumi atatu, pambuiu,
osalekanitsa, monga kuti ku panga lonjezano la tshabe. Kuti 18
ngati kuloeza kuli ndi mau, sikuli inso ndi lonjezano: koma
Mulungu anakupatsa ku Abraham ndi lonjezano. Ndimo 19
mau ali tshiani? Anaong'khetsedwa tshifuka tsha matshimo,
kwa ntawi mbeu ikafika kwa yomwe lonjezano lapangidwa;
*ndimo li*nalik*idwa* mwa anjelo ndi dzanja la mtetezi. Koma 20
mtetezi wosali *mtetezi* wa modzi; koma Mulungu ali modzi.
Kodi ndimo mau ali pa malonjezano a Mulungu? Si 21
tshointsho: kuti ngati mau anapatsidwa omwe anadziwa ku
panga ndi moyo, kudeka kukanakala nditu ndi mau. Koma 22
lemba latseka zintu zonse pansi pa mpulupulu, kuti lonje-
zano ndi mvanu m' Yesu Kristu linangopatsidwa kwa awo
omwe amvana.

Koma patsogolo mvanu unafika, tinasungidwa m' kudikira 23
pansi pa mau, tinatsekedwa kwa mvanu womwe ukanasonye-
zedwa pambuiu. Tshointsho kuti mau anali wotsogolera 24
mwana watu *ku tenga ife* kwa Kristu, kuti tinangodeketsedwa
ndi mvanu. Koma tsopano kuti mvanu unafika, sitiri inso 25
pansi pa wotsogolera mwana. Kuti inu muli nonse ana a 26

27 Mulungu, mwa mvanu, m' Kristu Yesu. Kuti monga ambiri
28 a inu anabapatizidwa m' Kristu munabvala Kristu. Kusa-
dziwa ku kala kapena Myuda kapena Mgrike, kusadziwa ku
kala kapena kapolo kapena mfulu, kusadziwa ku kala wama-
muna ndi wankazi: kuti muli nonse *muntu* modzi m' Kristu
29 Yesu. Ndimo ngati muli a Kristu, pomwe muli mbeu ya
Abraham, oloa kwa lonjezano.

4 Koma dinena kuti monga ntawi yambiri monga woloa ali
mwana, asia palibe kwa kapolo, ngati ali mwini wa onse;
2 koma ali pansi pa odikira ndi adindo kwa ntawi inaikidwa
3 ndi atate. Tshointsho ife enso, ntawi tinali ana, tinagwidwa
4 m' umpawi pansi pa zoiamba za dziko: koma ntawi kudzaza
kwa ntawi kunafika, Mulungu natumiza Mwana watshi,
5 wobadwa ndi nkazi, wabadwa pansi pa mau, kuti anango-
ombola awo omwe anali pansi pa mau, kuti tinangolandira
6 kulera kwa ana. Ndimo tshifuka muli ana, Mulungu
natumiza Nzimu wa Mwana watshi m' mitima yatu, kupfula,
7 Aba, Atate. Tshointsho kuti siuli ntawi ina kapolo, koma
mwana; ndimo ngati mwana, pomwe woloa mwa Mulungu.
8 Koma pa ntawi imene, sikudziwa Mulungu, munali
mumpawi ku iyo yomwe ndi makalidwe siiri milungu:
9 koma tsopano kuti munadziwa Mulungu, kapena kopambana
ku dziwidwa ndi Mulungu, bwanje mutembenuka anso kwa
zoiamba zofoka ndi zosauka, kwa zomwe mufuna ku kala
10 m' umpawi inso? Musunga masiku, ndi miezi, ndi zinsiku,
11 ndi dzaka. Diopa kwa inu, kani ndi kantu dapatsa ntshito
pa inu kwa tshabe.
12 Dipempa inu, abali, kalani monga di*ri*, kuti di*ri* monga
13 mu*li*. Simunatshimwa ndi ine: koma mudziwa kuti
tshifuka tsha kufoka kwa nyama dinauza ivangeli kwa inu
14 ntawi yoiamba: ndimo kumene komwe kunali kuyesa kwa
inu m' nyama yanga musanyoza, kapena musataia; koma
munalandira ine monga njelo wa Mulungu, *inde* monga
15 Kristu Yesu. Ndimo kuli kuti kudzisekererana kumene?
kuti dimariza ndi inu, kuti, ngati kuli kuta, mukanatshotsa
16 maso anu ndimo mukanapatsa awo kwa ine. Ndimo
tshointshi kodi dikala liwongo lanu, tshifuka diuza inu
17 nteradi? Afuna inu kwatshitsanzo m' njira palibe yabwino;
iai, afuna ku tsekera inu kunja, kuti mungofuna awo.
18 Koma tshiri tshabwino ku funidwa kwatshitsanzo m' tshintu
tshabwino pa ntawi zonse, ndimo si koka ntawi diri ndi inu.
19 Tiana tanga, ndi tomwe diri inso m' kubala kwa ntawi

Kristu apangidwa mwa inu, inde, dikafuna ku kala ndi 20
nu tsopano, ndi ku sinta liu langa; kuti diganizaganiza
ndi inu.

Uzani ine, inu nomwe mufuna ku kala pansi pa mau, 21
kodi simumva mau? Kuti alembedwa, kuti Abraham anali 22
ndi ana awiri, modzi ndi ndzakazi, ndi modzi ndi fulu-
yeikazi. Koma *mwana* ndi ndzakazi abadwa pambuiu 23
nyama; koma *mwana* ndi fuluyeikazi *abadwa* mwa lonjezano.
Zintu zimene ziri fanizo-lalikuru: kuti *akazi* amene ali 24
mapangano awiri; modzi kwa piri la Sinai, kubala ana kwa
umpawi, lomwe liri Hagare. Ndimo Hagare amene ali piri 25
la Sinai m' Arabe, ndimo lifanira ndi Yerusalem womwe uli
tsopano: kuti uli m' umpawi ndi ana atshi. Koma 26
Yerusalem womwe uli kumwamba uli woufulu, womwe uli
amai atu. Kuti alembedwa, 27

Tsekera, tshimbwira iwe emwe wosabala;
Pfula ndi kulira, iwe emwe usapwetekwa:
Kuti ambiri ali ana a wadzinja opambana emwe ali
ndi mamuna.

Ndimo ife, abali, monga Yisake anali, tiri ana a lonjezano. 28
Koma monga pomwe iemwe anabadwa pambuiu nyama 29
nazunza ie *emwe wabadwa* pambuiu Nzimu, inde tshointsho
kuli tsopano. Koma lemba linena tshiani? Turutsa ndza- 30
kazi ndi mwana watshi: kuti mwana wa ndzakazi sadzaloa
m' nyumba ndi mwana wa fuluyeikazi. Mwa kuti, abali, 31
sitiri ana a ndzakazi, koma a fuluyeikazi. Ndi ufulu 5
Kristu anatipanga ife aufulu: ndimo imani kolimba, ndimo
musakodwa anso m' tshigologolo tsha umpawi.

Ona, ine Paulos dinena ndi inu, kuti, ngati mulandira 2
kudula, Kristu sadzapindula inu kantu. Inde, dimariza 3
anso ku antu onse omwe alandira kudula, kuti ali ogong'gole
ku tshita mau onse. Mupangidwa tshabe kwa Kristu, inu 4
nomwe mufuna ku deketsedwa ndi mau; munagwa kwa
kufatsa. Kuti ife mwa Nzimu ndi mvanu tilinda kwa 5
kulingalira kwa kudeka. Kuti mwa Kristu Yesu kapena 6
kudula kusawerenga kantu, kapena kusadula; koma mvanu
kutshita mwa kukonda. Munalikutamanga bwino; watshe- 7
dwetsa inu ndani kuti musakamvera nteradi? Kuka- 8
ntshizira kumene kusana*fika* kwa iemwe aitana inu. Fumba 9
yeing'ono itupitsa buma lonse. Dipotshera mvanu kwa inu 10
m' Mwini, kuti musadzakala ndi muwongo wina: koma
iemwe abvuta inu adzamva kuweruza kwatshi, iemwe ali.

11 Koma ine, abali, ngati kosuntira diuza kudula, bwanje
dizunzidwa kosuntira? pomwe kukwiitsa kwa nkhwitshi
12 kwatshotsedwa. Difuna kuti awo omwe asokaniza inu inde
akadzidula.
13 Kuti inu, abali, munaitanidwa kwa ufulu; koka musa-
*tshita* ndi ufulu wanu kwa tshifukwa kwa nyama, koma
14 mwa kukonda imiriranani. Kuti mau onse adzazidwa m'
mau amodzi, *inde* m' amene; Udzakonda woiandikila wako
15 monga iwe eka. Koma ngati muluma ndi ku meza
modzi ndi wina, yang'anirani kuti musamarizidwa modzi ndi
wina.
16 Koma dinena, Endani ndi Nzimu, ndimo musadzaza kufuna
17 kwa nyama. Kuti nyama ifuna pa Nzimu, ndi Nzimu pa
nyama; kuti zimene zilingana umodzi ndi ina; kuti
18 musangotshita zintu zomwe mufuna. Koma ngati mutsogo-
19 zedwa ndi Nzimu, musali pansi pa mau. Koma ntshito
za nyama zisonyezedwa, zomwe ziri *zimenezi*, dama, kusatsuka,
20 kufuna tshigololo, kupembedza mafano, umabisalira,
makwio, ndeu, zinsanje, makwiiro, malekanitso, magawano,
21 zinjiru, madano, kuledzera, kubvina kwambiri, ndi zotere:
ndi zomwe ditshenjeza inu patsogolo, inde monga dina-
tshenjeza inu patsogolo, kuti awo omwe atshita zintu zotere
22 sadzaloa m' dziko la Mulungu. Koma dzobala dza Nzimu
dziri kukonda, tshimwemwe, ntendere, kumva kutali, kukoma,
23 ubwino, kumvana, kuanja, kudziweruza: pa zotere palibe
24 mau. Ndimo awo omwe ali a Kristu Yesu anapatshika
nyama ndi kumva ndi mafuno.
25 Ngati tikala ndi moyo ndi Nzimu, ndi Nzimu tiende enso.
26 Sitikale odzitama, kuputana, kudana modzi ndi wina.
6 Abali, inde ngati muntu apitiriridwa m' tshimo tshimodzi,
inu nomwe muli anzimu, bwezani modzi wotere m' nzimu
wa kuanja; kuyang'ana kwa iwe eka, kani iwe enso uyesedwa.
2 Nyamulani akatundu a modzi ndi wina, ndimo tshointsho
3 dzazani mau a Kristu. Kuti ngati muntu aganiza ie eka
4 ali kantu, ntawi ali watshabe, adzinyenga. Koma antu onse
ayese ntshito zao, ndimo pomwe adzapotshera kupambana
5 kwao ndi awo oka, ndimo si ndi ena. Kuti antu onse
adzanyamula akatundu ao.
6 Koma iemwe apunzitsidwa m' mau apatse kwa emwe
7 apunzitsa m' zintu zonse zabwino. Musanyengedwa;
Mulungu wosanyozedwa: kuti tshomwe muntu afesa,
8 tshomwe enso adzatema. Kuti iemwe afesa kwa nyama

yatshi kwa nyama adzatema kubvunda; koma iemwe afesa
kwa Nzimu adzatema kwa Nzimu moyo wosamariza.
Ndimo lekani ife sikulemetsedwa m' kutshita bwino: kuti 9
m' ntawi yabwino tidzatema, ngati sitifoka. Ndimo 10
tshointsho, monga tiri ndi pofatsa, titshite tshimene tshomwe
tshiri tshabwino kwa antu onse, ndi kopambana kwa awo
omwe ali a banja la mvanu.

Onani ndi malemba akuru bwanje dalemba kwa inu ndi 11
dzanja langa. Monga ambiri monga afuna ku panga sonyezo 12
labwino m' nyama, afulumiza inu ku dulidwa; koka kuti
osangozunzidwa kwa nkhwitshi ya Kristu. Kuti si inde 13
awo omwe alandira kudula asunga awo oka mau; koma
afuna ku potshera inu odulidwa, kuti angopambana m'
nyama yanu. Koma kukale kutali kwa ine ku pambana, koma 14
m' nkhwitshi ya Mwini watu Yesu Kristu, mwa yomwe dziko
lapatshikidwa kwa ine, ndi ine kwa dziko. Kuti kapena 15
kudula sikuli kantu, kapena kusadula, koma wopangidwa
watsopano. Ndimo monga ambiri monga adzaendaenda 16
ndi mulinganizo umene, ntendere *ukale* pa awo, ndi nsisi,
ndi pa Sirayeli la Mulungu.

Kwa ntawi yatsopano palibe muntu abvute ine: kuti dimva 17
kuotshedwa pa tupi langa malemba a Yesu.

Kufatsa kwa Mwini watu Yesu Kristu kukale ndi nzimu 18
wanu, abali. Amen.

---

EPISTOLA LA PAULOS KWA

# AFESO.

PAULOS, mpostile wa Kristu Yesu mwa kufuna kwa 1
Mulungu, kwa oyera omwe ali pa Feso, ndi amvanu
m' Kristu Yesu: Kufatsa kwa inu ndi ntendere kwa 2
Mulungu Atatu atu ndi Mwini Yesu Kristu.

Wodala *ali* Mulungu ndi Atate wa Mwini watu Yesu 3
Kristu, emwe anadalitsa ife ndi madalitso onse anzimu m'
*malo* akumwamba m' Kristu: inde monga nasang'ka ife 4
mwa ie patsogolo pa kuzika kwa dziko, kuti tikakala oyera
ndi opanda tshirama patsogolo pa ie m' kukonda: kunaika 5

kali ife kwa kulera monga ana mwa Yesu Kristu kwa ie
6 eka, kwa kusekera kwabwino kwa kufuna kwatshi, kwa
kulemekeza kwa kupambana kwa kufatsa kwatshi, komwe
7 napatsa kolere pa ife m' Wondikonda: mwa emwe tipo-
tshera kuomboledwa kwatu mwa mwazi watshi, kukululu-
kidwa kwa matshimo atu, kwa zolemera za kufatsa kwatshi,
8 zomwe anazipanga ku tshuruka kwa ife m' nzeru zonse ndi
9 tshisao, kunadziwitswa kwa ife kusadziwika kwa kufuna
10 kwatshi, kwa kusekera kwabwino kwatshi komwe anayere-
keza mwa ie kwa kuweruza kwa kudzaza kwa zinsiku,
ku ong'khetsa zintu zonse m' Kristu, zintu m' miamba,
11 ndi zintu pa pansi; mwa ie, *dinena*, mwa emwe enso tina-
pangidwa zoloa, kunaikidwa kali kwa kuyerekeza kwa ie
emwe atshita zintu zonse pambuiu pa kugazitsana kwa
12 kufuna kwatshi; kwa nsonga kuti tikakala kwa kulemekeza
kwa kupambana kwatshi, ife tomwe tinalingalira kali m'
13 Kristu: mwa emwe inu nonse, munamva mau a nteradi,
ivangeli wa kupulumutsa kwanu,—mwa emwe, munamvana
anso, munasindikizidwa ndi Nzimu Woyera wa lonjezano,
14 womwe uli tshigwiriro tsha zoloa zatu, kwa kuomboledwa
kwa kwatshi *kwa Mulungu*, kwa kulemekeza kwa kupambana
kwatshi.
15 Kwa tshifukwa tshimene ine enso, kunamva ndi mvanu
m' Mwini Yesu womwe uli mwa inu, ndi womwe *musonyeza*
16 kwa oyera onse, sindileka ku patsa tshakoma kwa inu,
17 kunena *ndi inu* m' mapempero anga; kuti Mulungu wa
Mwini watu Yesu Kristu, Atate wa kupambana, angopatsa
kwa inu nzimu wa nzeru ndi wa kusonyeza m' kudziwa
18 kwa ie; kupotshera maso a mitima yanu anaunikidwa, kuti
mungodziwa tshiani tshiri kulingalira kwa kuitana kwatshi,
tshiani zolemera za kupambana kwa zoloa zatshi m' oyera,
19 ndi tshiani ukuru woukuru wa mpamvu yatshi kwa ife
tomwe timvana, kwa kutshita kumene kwa mpamvu ya
20 kulimba kwatshi komwe anatshita m' Kristu, ntawi anaukitsa
ie kwa akufa, napanga ie ku kala pa dzanja latshi lamanja
21 m' *malo* akumwamba, kutali kumwamba ufumu wonse, ndi
kuweruza, ndi mpamvu, ndi umwini, ndi maina onse omwe
atshedwa, si koka m' kugonera kumene, koma anso m'
22 kumene komwe kulinkudza: ndimo naika zintu zonse
pansi pa mapazi atshi, ndimo napatsa ie ku kala mutu
23 pamwamba pa zintu zonse kwa eklesia, lomwe liri tupi
latshi, kudzaza kwa ie emwe adzaza zonse mwa zonse.

Ndimo inu *anafulumiza*, ntawi munali akufa mwa matshi- 2
mo ndi mpulupulu zanu, momwe ntawi yakali munapita 2
kwa kugonera kwa dziko limene, kwa woweruza wa mpamvu
ya mlengalenga, wa nzimu womwe tsopano utshita mwa
ana a kusamvera; mwa omwe ife tonse enso ntawi imodzi 3
tinakala m' mafuno a nyama yatu, kutshita mafuno a nyama
ndi a maganizo, ndimo tinali ndi makalidwe ana a kukwiira,
inde monga otsala:—koma Mulungu, ali wolemera m' nsisi, 4
kwa kukonda kwakukuru kwatshi ndi komwe nakonda ife,
inde ntawi tinali akufa mwa matshimo atu, natifulumiza 5
ndi Kristu (ndi kufatsa mwapulumutsidwa), ndimo anau- 6
kitsa ife ndi ie, ndimo napanga ife ku kala nai' m' *malo*
akumwamba, m' Kristu Yesu: kuti m' magonero alinkudza 7
anangosonyeza zolemera zazikuru za kufatsa kwatshi m'
kukoma kwa ife m' Kristu Yesu: kuti ndi kufatsa mwapu- 8
lumutsidwa mwa mvanu; ndimo kumene si kwa inu noka:
*kuli* ntulo wa Mulungu: si kwa zintshito, kuti palibe muntu 9
akapambana. Kuti tiri ntshito yatshi, tinapangidwa m' 10
Kristu Yesu kwa ntshito zabwino, zomwe Mulungu anafoto-
koza kali kuti tikapita mwa izo.

Mwa kuti kumbukilani, kuti ntawi yakali inu, Mitundu 11
m' nyama, yomwe itshedwa Kusadula ndi ilo lomwe litshe-
dwa Kudula, m' nyama, kupangidwa ndi manja; kuti 12
munali pa ntawi imene ogawidwa kwa Kristu, opangidwa
alendo kwa kuweruza kwa Sirayeli, ndi alendo kwa mapa-
ngano a lonjezano, kupotshera kulibe kulingalira ndimo
opanda Mulungu m' dziko. Koma tsopano m' Kristu Yesu 13
inu nomwe kali munali kutali munapangidwa kufupi
m' mwazi wa Kristu. Kuti ie ali ntendere watu, emwe 14
anapanga awiri modzi, nagwetsa koma lapakati lakugawa,
kunatshotsa m' nyama yatshi kukwia, *inde* mau a mau 15
*alandiridwa* m' maloezo; kuti anangopanga mwa ie eka wa
awiri muntu modzi watsopano, *tshointsho* kupanga ntendere;
ndimo anangoanjana awo awiri m' tupi limodzi kwa 16
Mulungu mwa nkhwitshi, kunapa kukwia mwa iyo: ndimo 17
nafika nauza ntendere kwa inu nomwe munali kutali, ndimo
ntendere kwa awo omwe anali kufupi: kuti mwa ie ife 18
awiri tipotshera kufika kwatu m' Nzimu umodzi kwa Atate.
Ndimo tshointshi simuli ntawi ina alendo ndi aulendo, koma 19
muli amzinda anzao ndi oyera, ndimo a banja la Mulungu,
kumangidwa pa kuzika kwa apostile ndi aprofeti, Kristu 20
Yesu ie eka ali mwala woukuru wa ngondia; mwa emwe 21

mamango onse, analumikizidwa bwino, akula m' malo oyera
22 m' Mwini; mwa emwe inu unso mumanganidwa kwa malo
a Mulungu m' Nzimu.
3 Kwa tshifukwa tshimene ine Paulos, womangidwa wa
2 Kristu Yesu kwa inu Mitundu,—ngati kuli tshointsho kuti
munamva ndi udindo wa kufatsa kumene kwa Mulungu
3 komwe kunapatsidwa ine kwa inu; bwanje kuti ndi ku-
sonyeza kunadziwitsidwa kwa ine kusadziwika, monga
4 dinalemba kali m' mau owereng'jeka, mwa kuti, ntawi
muwerenga, mudziwa ku dziwitsa kudziwa kwanga m' ku-
5 sadziwika kwa Kristu; komwe m' mafuko ena kusadziwitsi-
dwa kwa ana a antu, monga kwasonyezedwa kwatsopano
6 kwa apostile oyera atshi ndi aprofeti m' Nzimu; *inde*, kuti
Mitundu iri oloa anzao, ndi dziwalo anzao dza tupi, ndi
ogawana anzao a lonjezano m' Kristu Yesu mwa ivangeli,
7 ndi womwe dinapangidwa woimirira, kwa ntulo wa kufatsa
kwa Mulungu komwe kunapatsidwa kwa ine kwa kutshita
8 kwa mpamvu yatshi. Kwa ine, emwe diri wang'ono ndi
wang'ono wopambana wa oyera onse, kufatsa kumene kuna-
patsidwa, ku uza kwa Mitundu zolemera zosafunika za
9 Kristu; ndi ku panga antu onse ku ona tshiani tshiri
udindo wa kusadziwika komwe kwa magonero onse kwa-
10 bisidwa m' Mulungu emwe anapanga zintu zonse; monga
kuti tsopano kwa maufumu ndi zimpamvu m' *malo* aku-
mwamba inangodziwitsidwa mwa eklesia nzeru yopinduli-
11 dwa ya Mulungu, kwa kuyerekeza kwa magonero komwe
12 anayerekeza m' Kristu Yesu Mwini watu: mwa emwe
tipotshera kulimbika ndi kufika m' kumvana mwa mvanu
13 watu mwa ie. Mwa kuti difunsa kuti musafoka pa ma-
sautso anga kwa inu, omwe ali kupambana kwanu.
14, 15 Kwa tshifukwa tshimene digwada kwa Atate, kwa
emwe utate wonse mwa mwamba ndi pansi utshedwa,
16 kuti akapatsa inu, kwa zolemera za kupambana kwatshi,
kuti mungolimbitsidwa ndi mpamvu mwa Nzimu watshi
17 m' unzimu; kuti Kristu angokala m' mitima yanu mwa
mvanu; monga kuti inu, muli osindidwa ndi ozikidwa
18 m' kukonda, mungokala olimba ku dziwitsa ndi oyera onse
19 zomwe ziri kupingasa ndi utali ndi kuzuka ndi kuya, ndimo
ku dziwa kukonda kwa Kristu komwe kupitirira kudziwa,
kuti mungodzazidwa kwa kudzaza konse kwa Mulungu.
20 Ndimo kwa ie emwe ali ndi mpamvu ku tshita kutshuruka
kwambiri kopambana konse komwe tifunsa kapena tiganiza,

kwa mpamvu yomwe itshita mwa ife, kwa ie *kuli* kupa- 21
mbana m' eklesia ndi m' Kristu Yesu kwa mafuko onse a
kugonera kwa magonero. Amen.

Ndimo ine, womangidwa m' Mwini, dipempa inu ku enda 4
koenera kwa kuitana ndi komwe munaitanidwa, ndi kusa- 2
dzitama konse ndi kuyanja, ndi kumva kutali, kulekerezana
m' kukonda; kupatsa tshangu ku sunga umodzi wa Nzimu 3
m' tshomangira tsha ntendere. *Kuli* tupi limodzi, ndi 4
Nzimu umodzi, inde monga anso munaitanidwa m' kulinga-
lira kumodzi kwa kuitana kwanu; Mwini modzi, mvanu 5
umodzi, mbapatisma limodzi, Mulungu modzi ndi Atate a 6
onse, emwe ali pamwamba onse, ndi mwa onse, ndi mu onse.
Koma kwa ife tonse kufatsa kunapatsidwa kwa muyezo wa 7
ntulo wa Kristu. Mwa kuti ati, 8

Ntawi nakwera pamwamba, nagwira nkoli umpawi,
Napatsa mitulo kwa antu.

(Ndimo tshimene, Nakwera, tshiri tshiani koma kuti inso 9
natsika m' malo apansi a dziko? Iemwe anatsika ali 10
emwe enso emwe anakwera kutali kumwamba miamba
yonse, kuti anangodzaza zintu zonse.) Ndimo napatsa ena 11
*ku kala* apostile; ndi ena, aprofeti; ndi ena, aevangeli; ndi
ena, abusa ndi apunzitsi; kwa kuta kwa oyera, kwa ntshito 12
ya kuimirira, kwa kumanga kwa tupi la Kristu: kwa ntawi 13
ife tonse tifika kwa umodzi wa mvanu, ndi kwa kudziwa
kwa Mwana wa Mulungu, kwa mkuru, kwa mulinganizo wa
msing'ku wa kudzaza kwa Kristu: kuti sitingokala ntawi 14
ina ana, kuponyedwa kwina ndi kwina nanyamulidwa
kozungulira ndi mpepo yonse ya kupunzitsa, ndi tsenga la
antu, m' kutshenjera, pambuiu pa matshenjero a kutshi-
mwa; koma kunena nteradi m' kukonda, tingokula m' zintu 15
zonse mwa ie, emwe ali mutu, *inde* Kristu; kwa emwe tupi 16
lonse linalumikizidwa bwino ndi linagwirizanidwa mwa itsho
tshomwe mfundo zonse zikwanira, kwa kutshita m' mulinga-
nizo wa mapande onse oanjanitswa, kupanga kukula kwa tupi
kwa kumanga kwa ilo loka m' kukonda.

Ndimo dinena tshimene, ndimariza m' Mwini, kuti musa- 17
enda ntawi ina monga Mitundu unso iendа, m' utsiru wa
muwongo wao, kudetsedwa m' kudziwitsa kwao, kupangidwa 18
alendo kwa moyo wa Mulungu tshifuka tsha kupulukira
komwe kuli mwao, tshifuka tsha kulimbitsa kwa mitima yao;
omwe ali opanda kumva anadzipatsa kwa kufuna tshigololo; 19
ku tshita kusatsuka konse ndi kuumira. Koma musana- 20

21 punzira tshointsho Kristu; ngati tshingokala kuti munamva
ie, ndimo munapunzitsidwa mwa ie, inde monga nteradi uli
22 m' Yesu: kuti mutshotsa, monga kwa makalidwe a moyo
akali anu, muntu wakali, emwe akula wobvunda pambuiu
23 mafuno a tshinyengo; ndimo kuti mungofotokozedwa mu
24 nzimu wa muwongo wanu, ndimo muika muntu watsopano,
emwe pambuiu Mulungu wapangidwa m' kudeka ndi kuyera
kwa nteradi.
25 Mwa kuti, kutshotsa kunama, lankulani nteradi inu nonse
ndi oiandikila anu: kuti tiri dziwalo modzi wa wina.
26 Kwiirani, ndimo musatshimwa: musaleka dzua ku loa pa
27 kukwiira kwanu: kapena musapatsa malo ku diabolos.
28 Leka iemwe anaba sikuba ntawi ina: koma kopambana
atshite, kutshita ndi manja atshi tshintu tshomwe tshiri
tshabwino, kuti angopotshera mwa komwe ku patsa kwa ie
29 emwe ali ndi kufunidwa. Leka kulibe kunena kwaku-
bvunda ku turuka kwa nkamwa mwanu, koma kotere monga
kuli kwabwino kwa kumanga monga kufunidwa kungokala,
30 kuti kungopatsa kufatsa kwa awo omwe amva. Ndimo
musamvetsa tshisoni Nzimu Woyera wa Mulungu, mwa
31 womwe munasindikizidwa kwa siku la kuombola. Zonse
kupsa ntima, ndi kukwiira, ndi kukwia, ndi kulongolola,
ndi kunyoza, zitshotsedwe kwa inu, ndi madano onse:
32 ndimo kalani okoma modzi ndi wina, ogwa ntima, kululu-
kiranani, inde monga Mulungu unso mwa Kristu anakululu-
kira inu.

5 Ndimo kalani ofanizira a Mulungu, monga ana okonde-
2 dwa; ndimo endani m' kukonda, inde monga Kristu unso
anakonda inu, nadzipereka kwa ife, tshotsira ndi nsembe
kwa Mulungu kwa fungo la tshonung'kira tshabwino.
3 Koma dama ndi kusatsuka konse, kapena kusirira, leka iko
inde sikutshulidwa mwa inu, monga kuenera oyera;
4 kapena kunyansa, kapena kulankula kwakupusa, kapena
kusetsa, zomwe zosali zabwino: koma kopambana kupatsa
5 tshakoma. Kuti tshimene mudziwa nditu, kuti palibe
wodama, kapena muntu wosatsuka, kapena muntu wosirira,
emwe ali wopembedza mafano, apotshera zoloa m' dziko la
6 Kristu ndi Mulungu. Palibe muntu anyenge inu ndi mau
atshabe: kuti tshifuka tsha zintu zimenezi kufika kukwiira
7 kwa Mulungu pa ana a kusamvera. Ndimo musakala
8 ogawana ndi awo; kuti munali ntawi imodzi ndima, koma
tsopano muli kuunika m' Mwini: endani monga ana a

kuunika (kuti tshobala tsha kuunika tshiri m' ubwino 9
wonse ndi kudeka ndi nteradi), kuyesa tshomwe tshiri 10
kusekera kwabwino kwa Mwini; ndimo musapotshera 11
palibe unzao ndi ntshito zosabala za ndima, koma kopa-
mbana inde sulumulani izo; kuti zintu zomwe zitshitidwa 12
ndi awo kutseri ali manyazi inde ku nena nazo. Koma 13
zintu zonse ntawi zisulumulidwa zisonyezedwa ndi kuunika:
kuti zintu zonse zomwe zisonyezedwa ziri kuunika. Mwa 14
kuti anena, Uka, iwe emwe ugona tulo, ndimo ukirira kwa
akufa, ndimo Kristu adzawala pa iwe.

Ndimo yang'anirani bwino bwanje muenda, si monga 15
opanda nzeru, koma monga anzeru; kuombola ntawi, 16
tshifuka masiku ali oipa. Mwa kuti musakala opusa, koma 17
dziwani komwe kufuna kwa Mwini kuli. Ndimo musa- 18
ledzera ndi vinyo, momwe kulipo kusaruka, koma dzazi-
dwani ndi Nzimu; kulankula modzi ndi wina m' masalmo 19
ndi zinyimbo ndi zinyimbo zanzimu, kuimba ndi kupanga
msao m' mitima yanu kwa Mwini; kupatsa tshakoma 20
ntawi yonse kwa zintu zonse m' dzina la Mwini watu Yesu
Kristu kwa Mulungu, inde Atate; kudziika pansi modzi ndi 21
wina m' kuopa kwa Kristu.

Akazi, *kalani pansi pa* amuna anu, monga kwa Mwini. 22
Kuti mamuna ali mutu wa nkazi, monga Kristu unso ali 23
mutu wa eklesia, *ali* ie eka mpulumutsi wa tupi. Koma 24
monga eklesia liri pansi pa Kristu, tshointsho akazi inso
*akale* kwa amuna ao m' zintu zonse. Amuna, kondani 25
akazi anu, inde monga Kristu unso nakonda eklesia, nadzi-
pereka kwa ilo; kuti anangoyeretsa ilo, kunasambitsa ilo 26
ndi kutsuka kwa madzi ndi mau, kuti anangopereka eklesia 27
kwa ie eka *eklesia* la kupambana, losali ndi banga kapena
tsinya kapena tshintu tshina tshotere; koma kuti likakala
loyera ndi lopanda tshirama. Inde tshointsho amuna 28
akanakonda anso akazi ao monga matupi ao. Iemwe akonda
nkazi watshi adzikonda: kuti palibe muntu ntawi yapita 29
nakwiira nyama yatshi; koma ailera naisunga, inde monga
Kristu unso eklesia; tshifuka tiri dziwalo dza tupi latshi. 30
Kwa tshifukwa tshimene muntu adzasia atatu atshi ndi amai 31
atshi, ndimo adzagwirizana ndi nkazi watshi; ndimo awiri
adzakala nyama imodzi. Kusadziwika kumene kuli kwa- 32
kukuru: koma dinena ndi Kristu ndimo ndi eklesia. Koma 33
onse kondani inso koanjanitswa akazi anu inde monga inu
noka; ndimo nkazi *aone* kuti aope mamuna watshi.

6 Ana, mverani atatu anu ndi amai anu m' Mwini: kuti
2 tshimene tshiri tshabwino. Lemekeza atatu ako ndi amai
3 ako (omwe ali mau atshimodzi ndi lonjezano), kuti kungo-
kala bwino ndi iwe, ndimo ungokala ndi moyo woutali pa
4 dziko. Ndimo, inu atate, musaputa ana anu kwa kukwiira:
koma lerani awo m' kusulumula ndi kuambirira kwa Mwini.
5 Akapolo, mverani awo omwe kwa nyama ali enı anu,
ndi kuopa ndi kuntentemera, m' umodzi wa mitima yanu,
6 monga kwa Kristu; si m' njira ya kutshita-pa-maso, monga
oseketsa a antu; koma monga akapolo a Kristu, kutshita
7 kufuna kwa Mulungu kwa ntima; ndi kufuna kwabwino
8 kuimirira, monga kwa Mwini, ndimo si kwa antu: kudziwa
kuti tshintu tshabwino tshomwe onse atshita, tshomwe
adzalandira anso kwa Mwini, kapena *ali* kapolo kapena
9 mfulu. Ndimo, eni inu, tshitani zintu zimenezi kwa awo,
ndimo lekani kuopetsa: kudziwa kuti Mwini wao ndi wanu
ali m' mwamba, ndimo ndi ie kulibe tsang'ko.
10 Kwakutungo, limbikitsidwani m' Mwini, ndimo m' mpa-
11 mvu ya kulimba kwatshi. Bvalani tshamuna tshonse tsha
Mulungu, kuti mungodziwa ku ima pa matshenjero a
12 diabolos. Kuti kulimbana kwatu sikuli pa nyama ndi
mwazi, koma pa maufumu, pa zimpamvu, pa oweruza a
dziko a ndima umene, pa *magulu* anzimu a mpulupulu m'
13 *malo* akumwamba. Mwa kuti tukulani tshamuna tshonse
tsha Mulungu, kuti mungodziwa ku kaniza m' siku loipa,
14 ndimo, kunatshita konse, ku ima. Ndimo imani, kuna-
mangidwa mtshuuno mwanu ndi nteradi, ndi kunabvala
15 tshotshinjiriza tsha kudeka, ndimo kunabvala mapazi anu
16 ndi kufotokoza kwa ivangeli wa ntendere; m' zonse kutu-
kula tshikopa tsha mvanu, ndi tshomwe mudzakala ndi
mpamvu ku zima mibvi ya moto yonse ya *wa*mpulupulu.
17 Ndimo tengani tshisoti tsha kupulumutsa, ndi mpeni wa
18 nkondo wa Nzimu, womwe uli mau a Mulungu: ndi
kupempera konse ndi kupempera, kupempera pa nsiku
zonse m' Nzimu, ndi kudikira kwa iko m' kuyesabe konse
19 ndi kupempa kwa oyera onse, ndi kwa ine, kuti kutshula
kungopatsidwa kwa ine m' kutsegula nkamwa mwanga, ku
20 dziwitsa ndi kulimbika kusadziwika kwa ivangeli, kwa
komwe diri mtenga m' maunyolo; kuti mwa iwo dingonena
kolimbika, monga dikanalankula.
21 Koma kuti inu unso mungodziwa zintu zanga, bwanje
ditshita, Tikiko, mbali wokondedwa ndi woimirira wamvanu

m' Mwini, adzadziwitsa kwa inu zintu zonse: emwe datu- 22
miza kwa inu kwa kuyerekeza kumene nditu, kuti mungo-
dziwa makalidwe anu, ndimo kuti angosangalatsa mitima
yanu.

Ntendere uli kwa abali, ndi kukonda ndi mvanu, kwa 23
Mulungu Atate ndi Mwini Yesu Kristu. Kufatsa kuli ndi 24
awo onse omwe akonda Mwini watu Yesu Kristu m' kusa-
bvunda.

---

## EPISTOLA LA PAULOS KWA

# AFILIPI.

PAULOS ndi Timote, akapolo a Kristu Yesu, kwa oyera 1
onse m' Kristu Yesu omwe ali pa Filipi, ndi oya-
ng'anira ndi oimirira: Kufatsa kwa inu ndi ntendere kwa 2
Mulungu Atatu atu ndi Mwini Yesu Kristu.

Dinena tshakoma kwa Mulungu wanga pa kumbukila 3
kwanga konse pa inu, ntawi yonse m' mapempo anga onse 4
kwa inu nonse kupanga kupempa kwanga ndi tshimwemwe,
kwa unzanu m' kupititsa kwa ivangeli kwa dzua loamba 5
kwa ntawi yatsopano; kumvana ndi tshintu tshimene 6
nditu, kuti iemwe anaamba ntshito yabwino mwa inu adzaita
kwa dzua la Yesu Kristu: inde monga tshiri tshabwino kwa 7
ine ku kala ndi muwongo wotere kwa inu nonse, tshifuka
dipotshera inu m' ntima wanga, mwa ambiri monga, m'
zomangira zanga ndi m' kudzikana ndi kulimbikitsa kwa
ivangeli, muli nonse ogawana ndi ine ndi kufatsa. Kuti 8
Mulungu ali womariza wanga, bwanje difunitsa kwa inu
nonse m' nsisi zokoma za Kristu Yesu. Ndimo tshimene 9
dipempera, kuti kukonda kwanu kungotshuruka kosuntira
kuyenjezayenjeza m' kudziwa ndi kudziwitsa konse; kuti 10
mungosimba zintu zomwe ziri zopambana; kuti mungokala
oona ndi opanda tshimo kwa siku la Kristu; kudzazidwa 11
ndi dzobala dza kudeka, dzomwe dziri mwa Yesu Kristu,
kwa kupambana ndi kulemekeza kwa Mulungu.

Koma difuna inu ku dziwa, abali, kuti zintu *zomwe zina-* 12

*kala* kwa ine zinafika kopambana kwa kupitirira kwa
13 ivangeli; tshointsho kuti zomangira zanga zinasonyezedwa
m' Kristu m' gulu lonse la Pretorium, ndi kwa otsala onse;
14 ndimo kuti unyinji wa abali m' Mwini, kuli omvana mwa
zomangira zanga, ali olimbika opambana ku lankula mau a
15 Mulungu opanda kuopa. Ena nditu auza Kristu inde kwa
16 dano ndi ndeu; ndi ena anso kwa kufuna kwabwino: uyu
*atshitshita* kwa kukonda, kudziwa kuti diikidwa kwa kudzi-
17 kana kwa ivangeli: koma uyo auza Kristu kwa kugawa, si
koona, kuganiza ku ukitsa sautso kwa ine m' zomangira
18 zanga. Nanga tshiani? koka kuti m' njira zonse, kapena
m' tshinyengo kapena m' nteradi, Kristu auzidwa; ndi mwa
19 iko disekera, inde, ndidzasekera. Kuti didziwa kuti
tshimene tshidzatembenuka kwa kupulumutsa kwanga, mwa
kupempa kwanu ndi kukwanitsa kwa Nzimu wa Yesu
20 Kristu, kwa kuyang'anira kolimba kwanga ndi kulinga-
lira, kuti m' tshabe didzapatsidwa manyazi, koma *kuti* ndi
kulimbika konse, monga ntawi yonse, *tshointsho* tsopano onso
Kristu adzapambanitsidwa m' tupi langa, kapena ndi moyo,
21 kapena ndi imfa. Kuti kwa ine ku kala ndi moyo kuli
22 Kristu, ndi ku fa kuli kupindula. Koma ngati ku kala ndi
moyo m' nyama,—*ngati* tshimene tshiri tshobala tsha
ntshito yanga, pomwe tshomwe didzasang'ka sindidziwitsa.
23 Koma diri m' kusing'kasing'ka pakati pa ziwiri, diri ndi
kufuna ku muka ndi ku kala ndi Kristu; kuti kuli kwabwino
24 kwambiri kopambana nditu: koma ku kalabe m' nyama
25 kuli kufunidwa kopambana kwa inu. Ndimo kuli ndi ku-
mvana kumene, didziwa kuti didzakalabe, inde, ndi ku
kalabe ndi inu nonse, kwa kupitirira kwanu ndi tshimwemwe
26 m' mvanu; kuti kupambana kwanu kungotshuruka m'
Kristu Yesu mwa ine mwa kuona kwanga ndi inu unso.
27 Koka lekani makalidwe a moyo anu ku kāla koenera kwa
ivangeli wa Kristu: kuti, kapena difika ndi ku ona inu
kapena diribe, dingomva ndi makalidwe anu, kuti muima
kolimba m' Nzimu umodzi, ndi ntima umodzi ku yesa kwa
28 mvanu wa ivangeli; ndimo m' palibe kantu muopsedwa
ndi maliwongo: komwe kuli kwa awo tshizindikilo tsho-
onedwa tsha kumwaza, koma tsha kupulumutsa kwanu, ndi
29 tshimene kwa Mulungu; tshifuka kwa inu wapatsidwa
kwa Kristu, si koka ku mvana ndi ie, koma anso ku mva
30 kwa ie: kupotshera makangano amodzi omwe munaona
mwa ine, ndimo tsopano mumva ali mwa ine.

Ndimo ngati kulipo kusangalatsa kwina m' Kristu, ngati 2
kuiwaza kwina kwa kukonda, ngati unzatshi wina wa
Nzimu, ngati nsisi zokoma zina ndi zisoni, dzazani tshi- 2
mwemwe tshanga, kuti muli ndi muwongo umodzi, muli ndi
kukonda kumodzi, muli ndi kuanja kumodzi, ndi muwongo
umodzi; *kutshita* palibe kantu mwa kugawa kapena mwa 3
kudzitama, koma m' kusadzitama kwa muwongo onse kugani-
zana ena abwino opambana awo oka; si onse a inu ku- 4
yang'anira kwa zintu zanu, koma onse a inu unso kwa zintu
za ena. Kalani ndi muwongo umene mwa inu, womwe 5
unali inso m' Kristu Yesu: emwe, ali m' makalidwe a 6
Mulungu, sanatshiganiza tshosekeretsa ku kala pa umodzi
ndi Mulungu, koma nadzikutula, kutenga makalidwe a 7
kapolo, kukala m' kufaniza kwa antu; ndimo kupezedwa m' 8
makalidwe monga muntu, nadzitshepetsa, kukala wamvera
*inde* kwa imfa, e, imfa ya nkhwitshi. Mwa kuti inso Mulungu 9
wamtalikitsa kwakutali, napatsa kwa ie dzina lomwe liri
pamwamba pa maina onse; kuti m' dzina la Yesu maondo 10
onse akagwada, a *zintu* m' mwamba ndi pa dziko ndi pansi
pa dziko, ndimo kuti malilume onse akabvomera kuti Yesu 11
Kristu ali Mwini, kwa kupambana kwa Mulungu Atate.

Tshointsho kuti, okondedwa anga, inde monga mwamvera 12
ntawi zonse, si monga m' kuona kwanga koka, koma tsopano
kwambiri kopambana m' kulibe kwanga, tshitani kupulu-
mutsa kwanu ndi kuopa ndi kuntentemera; kuti ali 13
Mulungu emwe atshita mwa inu ku funa ndi ku tshita
kwa kusekeretsa kwabwino kwatshi. Tshitani zintu zonse 14
kopanda mandandaulo ndi makani; kuti mungokala kopanda 15
tshulo ndi osatshimwitsa, ana a Mulungu opanda tshirama
m' kati m' fuko lokotakota ndi losasamala, mwa omwe
muonedwa monga miuni m' dziko, kuturutsa mau a moyo; 16
kuti dingopotshera ndi kantu ku pambana m' dzua la Kristu,
kuti sindinatamanga m' tshabe kapena sindinatshita m'
tshabe. Inde, ndimo ngati ditsiridwa pa nsembe ndi 17
kuimirira kwa mvanu wanu, disekera, ndi kondwera ndi inu
nonse: ndimo m' njira imodzi inu unso musekera, ndi mu- 18
kondwera ndi ine.

Koma dilingalira m' Mwini Yesu ku tumiza Timote 19
nsanga kwa inu, kuti ine enso dingokala ndi kusangalala
kwabwino, ntawi didziwa makalidwe anu. Kuti sindipo- 20
tshera muntu ndi muwongo umodzi, emwe adzayang'anira
koona kwa makalidwe anu. Kuti awo onse afuna zao, si 21

22 zintu za Yesu Kristu. Koma mudziwa sonyezo la ie, kuti,
monga Mwana *aimirira* atate, *tshointsho* naimirira ndi ine
23 m' kupitirira kwa ivangeli. Ndimo ie dilingalira ku tumiza
nsanga, monga nsanga monga didzaona bwanje kudzakala
24 ndi ine: koma dimvana m' Mwini kuti ine ndeka anso
25 didzafika nsanga. Koma dinaganiza kufunidwa ku tumiza
kwa inu Pafrodito, mbali wanga ndi wotshita nzanga ndi
wankhondo nzanga, ndi mtenga wanu ndi woimirira kwa
26 kufuna kwanga; kwa ntawi nafunitsa pa inu nonse, nabvuti-
27 tsidwa, tshifuka munamva kuti anadwala: kuti nditu anali
wodwala pafupi ndi imfa: koma Mulungu anali ndi nsisi
pa ie; ndimo si pa ie eka, koma pa ine enso, kuti sindinango-
28 kala ndi tshisoni pa tshisoni. Ndimo damtumiza kwatshangu
kopambana, kuti, ntawi muona ie enso, mungosekera, ndimo
kuti dingokala ndi tshisoni tshatshing'ono tshopambana.
29 Ndimo landirani ie m' Mwini ndi tshimwemwe tshonse; ndi
30 ganiza ndi otere ndi ulemu: tshifuka kwa ntshito ya Kristu
nafika pafupi kwa imfa, kutaia moyo watshi ku kwanitsa
kumene komwe kunalikupanda m' kuimirira kwanu kwa ine.
3 Kwakutungo, abali anga, kalani bwino m' Mwini.
Kulemba zintu zimodzi kwa inu, kwa ine nditu sikuli
2 kolema, koma kwa inu kuli kopulumuka. Tshenjerani ndi
agaru, tshenjerani ndi otshita zoipa, tshenjerani ndi kudula:
3 kuti ife tiri kudula, tomwe tipembedza ndi Nzimu wa
Mulungu, ndimo tipambana m' Kristu Yesu, ndimo sitiri ndi
4 kumvana m' nyama: ngati ine ndeka dinangopotshera
kumvana inde m' nyama: ngati muntu wina aganiza ku
potshera kumvana m' nyama, ine kopambana nditu:
5 wodulidwa dzua latshisanu ndi tshitatu, wa kubadwa kwa
Sirayeli, wa fuko la Benyamin, Mhebere wa Ahebere;
6 monga ndi mau, Mfarisi; monga ndi utshitsanzo, kuzunza
eklesia; monga ndi kudeka komwe kuli m' mau, wopezedwa
7 wopanda tshulo. Koma zintu zomwe zinali kupindula kwa
8 ine, zimene daganiza kumwaza kwa Kristu. Inde nditu,
ndimo diganiza zintu zonse kuli kumwaza kwa ubwino wa
kudziwa kwa Kristu Yesu Mwini wanga: kwa emwe dinamva
9 kumwaza kwa zintu zonse, ndimo diganiza izo zotaia, kuti
dingopeza Kristu, ndimo dingopezedwa mwa ie, sikupotshera
kudeka kwa ine ndeka, *inde* kumene komwe kuli kwa mau,
koma kumene komwe kuli mwa mvanu mwa Kristu, kudeka
10 komwe kuli kwa Mulungu ndi mvanu: kuti dingodziwa ie,
ndi mpamvu ya kuukirira kwatshi, ndi unzatshi wa kumva

kwatshi, kukala kofanizidwa kwa imfa yatshi; ngati ndi 11
kantu dingofika kwa kuukirira kwa akufa. Si kuti dala- 12
ndira kali, kapena ditetsedwa kali : koma didzifulumiza,
ngati kungokala kuti dingodziwitsa kumene kwa komwe
enso dinadziwitsidwa ndi Kristu Yesu. Abali, sindidziganiza 13
kosuntira kunadziwitsa : koma tshintu tshimodzi *ditshita*,
kuiwala zintu zomwe ziri pambuiu, ndi kuturutsa patsogolo
kwa zintu zomwe ziri patsogolo, didzifulumiza kwa tshigwiro 14
kwa tshosekeretsa tsha kuitana kwa mwamba kwa Mulungu m'
Kristu Yesu. Ndimo ife, monga ambiri monga ali akuta, tikale 15
ndi muwongo wotere: ndimo ngati m'kantu muli ndi muwongo
wina, inde umene Mulungu adzasonyeza kwa inu: koka, kwa 16
pomwe tafika kali, ndi *mulinganizo* umene umodzi tiende.

Abali, kalani odzifanizirana a ine, ndimo yang'anirani awo 17
omwe aenda tshointsho inde monga mwapotshera ife kwa
sonyezo. Kuti ambiri aenda, ndi omwe dinauza inu ntawi 18
zambiri, ndimo tsopano diuza inu inde kulira nsozi, kuti *ali*
maliwongo a nkhwitshi ya Kristu : nsonga ya omwe iri 19
kumwaza, mulungu wa omwe ali mimba, ndi kupambana
kwa *omwe* ali m' manyazi ao, omwe asamala zintu za pansi.
Kuti umzinda watu uli m' mwamba; kwa komwe enso 20
tilindira kwa Mpulumutsi, Mwini Yesu Kristu: emwe adza- 21
panga anso tupi la kutshepetsedwa kwatu, *kuti lingo*fanizidwa
kwa tupi la kupambana kwatshi, kwa kutshita mwa komwe
ali ndi mpamvu inde ku ika pansi zintu zonse kwa ie eka.

Tshointsho kuti, abali anga okondedwa ndi ofunitsidwa, 4
tshimwemwe tshanga ndi tshisoti tshotshuka, tshointsho
imani m' Mwini, okondedwa anga.

Ditaulira Wodiya, ndimo ditaulira Sintike, ku kala ndi 2
muwongo umodzi m' Mwini. Inde, dipempa iwe enso, watshi- 3
gologolo nzanga woona, tangata akazi ameue, kuti anatshita
ndi ine m' ivangeli, ndi Klemento onso, ndi otsala a otshita
anzanga, maina a omwe ali m' buku la moyo.

Kalani bwino m' Mwini ntawi zonse: enso didzanena, 4
Kalani bwino. Lekani kuanja kwanu ku dziwidwa kwa 5
antu onse. Mwini ali pafupi. M' palibe kantu kalani 6
kofunsafunsa; koma m' zintu zonse ndi kupempera ndi
kupempa ndimo ndi kunena tshakoma mafunso anu adzi-
widwe kwa Mulungu. Ndimo ntendere wa Mulungu, 7
womwe upitirira kudziwitsa konse, kudzadikira mitima
yanu ndi maganizo anu m' Kristu Yesu.

Kwakutungo, abali, zintu zomwe ziri zanteradi, zintu 8

zomwe ziri zaulemu, zintu zomwe ziri zodeka, zintu zomwe
ziri zoyera, zintu zomwe ziri zabwino, zintu zomwe ziri
za mbiri yabwino; ngati ulipo umuntu wina, ndimo ngati
kulipo kulemekeza kwina, ganizani ndi zintu zimenezi.
9 Zintu zomwe munapunzira ndi munalandira ndi munamva
ndi munaona mwa ine, zintu zimenezi tshitani: ndi
Mulungu wa ntendere adzakala ndi inu.
10 Koma disekera kwambiri m' Mwini, kuti tsopano pomwe
mwafulumiza anso kuganiza kwanu kwa ine; mwa kuti
11 munaganiza nditu, koma munapanda pofatsa. Si kuti
dinena ndi kufunidwa: kuti dapunzira, m' makalidwe anje
12 diri, momwe ku kala kosekera. Didziwa bwanje ku tshepe-
tsedwa, ndimo didziwa anso bwanje ku tshuruka: m'
tshintu tshonse ndi m' zintu zonse dapunzira mtseri kudza-
zidwa ndi ku mva njala, ku tshuruka ndi ku funira.
13 Didziwa ku tshita zintu zonse mwa iemwe alimbikitsa ine.
14 Koma munatshita bwino, kuti munali ndi unzanu ndi sautso
15 yanga. Ndimo inu noka anso mudziwa, inu Afilipi, kuti m'
kuiamba kwa ivangeli, ntawi dinatshoka kwa Makedoniya,
palibe eklesia linali ndi unzanga ndi ine m' tshintu tsha kupa-
16 tsa ndi kulandira, koma inu noka; kuti inde m' Tesalonika
munatumiza kamodzi ndi kamodzi kwa kufunidwa kwanga.
17 Si kuti difunira ntulo; koma difunira tshobala tshomwe
18 tshikula kwa inu. Koma dipotshera zintu zonse, ndimo
ditshuruka: didzazidwa, kunalandira kwa Pafrodito zintu
*zomwe zinafika* kwa inu, fungo la tshonung'kira tshabwino,
nsembe yolandiridwa, yosekeretsa bwino kwa Mulungu.
19 Ndimo Mulungu wanga adzadzazitsa kufunidwa konse kwa
inu, kwa zolemera zatshi m' kupambana m' Kristu Yesu.
20 Ndimo kwa Mulungu watu ndi Atate *kukale* kupambana
kwa magonero a magonero. Amen.
21 Utsani oyera onse m' Kristu Yesu. Abali omwe ali ndi
22 ine autsa inu. Oyera onse autsa inu, kopambana awo omwe
ali a banja la Kesare.
23 Kufatsa kwa Mwini Yesu Kristu kukale ndi nzimu
wanu.

### EPISTOLA LA PAULOS KWA

# AKOLOSE.

PAULOS, mpostile wa Kristu Yesu mwa kufuna kwa 1
Mulungu, ndi Timote mbali watu, kwa oyera ndi 2
abali amvanu m' Kristu *omwe ali* pa Kolose: Kufatsa kwa
inu ndi ntendere kwa Mulungu Atatu atu.
Tinena tshakoma ku Mulungu Atate wa Mwini watu 3
Yesu Kristu, kupempera ntawi zonse kwa inu, kunamva 4
ndi mvanu wanu m' Kristu Yesu, ndimo ndi kukonda
komwe mupotshera kwa oyera onse, tshifuka tsha kuli- 5
ngalira komwe kuikidwa kwa inu m' miamba, ndi komwe
munamva kali m' mau a nteradi wa ivangeli, omwe anafika 6
kwa inu; inde monga ali inso m' dziko lonse kubala dzobala
ndi kukulitsa, monga *atshita* mwa inu unso, kwa siku
munamva ndi munadziwa kufatsa kwa Mulungu m' nteradi;
inde monga munapunzira kwa Epafra kapolo nzatu woko- 7
ndedwa, emwe ali woimirira wamvanu wa Kristu kwa ife,
emwe enso nauza kwa ife kukonda kwanu m' Nzimu. 8
Kwa tshifukwa tshimene ife enso, kwa dzua tinamva, 9
sitireka ku pempera ndi ku pempa kwa inu, kuti mungo-
dzazidwa ndi kudziwa kwa kufuna kwatshi m' nzeru ndi
kudziwa zonse zanzimu, ku enda koenera kwa Mwini kwa 10
kusekeretsa konse, kubala tshobala m' ntshito yonse yabwino,
ndi kukulitsa m' kudziwa kwa Mulungu; kulimbitsidwa 11
ndi mpamvu yonse, kwa kulimbika kwa kupambana kwatshi,
kwa kulongosola konse ndi kumva kutali ndi tshimwemwe;
kunena tshakoma kwa Atate, emwe anapanga ife oenera 12
kukala ogawana a kuloa kwa oyera m' kuunika; emwe 13
anapulumutsa ife kwa mpamvu ya ndima, ndimo nasintanitsa
ife mwa dziko la Mwana wa kukonda kwatshi; mwa emwe 14
tipotshera kuomboledwa kwatu, kukululukiridwa kwa zoipa
zatu: emwe ali fanizo la Mulungu wosaoneka, wobadwa 15
woiamba wa kupanga konse; kuti mwa ie zintu zonse 16
zinapangidwa, m' miamba ndi pa dziko, zintu zoonekedwa
ndi zintu zosaonekedwa, kapena mipando yotshuka kapena
umwini kapena maufumu kapena zimpamvu; zintu zonse

17 zinapangidwa mwa ie, ndi kwa ie; ndimo ali patsogolo pa
18 zintu zonse, ndimo mwa ie zintu zonse zikala. Ndimo ie ali
mutu wa tupi, eklesia: emwe ali kuiamba wobadwa woiamba
kwa akufa; kuti m' zintu zonse anangopotshera kupitirira
19 Kuti kunali kusekera kwabwino *kwa Atate* kuti mwa ie
20 kudzaza konse kukakala; ndimo mwa ie ku anjanitsa zintu
zonse kwa ie eka, kunapanga ntendere mwa mwazi wa
nkhwitshi yatshi; mwa ie, *dinena*, kapena zintu pa dziko,
21 kapena zintu m' miamba. Ndimo inu, m' ntawi yapita
munapangidwa alendo ndi maliwongo m' muwongo wanu m'
22 ntshito zoipa zanu, kosuntira tsopano waanjanitsa m' tupi la
nyama yatshi mwa imfa, ku pereka inu oyera ndi opanda
tshirama ndi osadziwa ku sulumulidwa patsogolo pa ie:
23 ngati kuli tshointsho kuti mukalabe m' mvanu, ozikidwa ndi
olimbika, ndimo si osuntidwa kwa kulingalira kwa ivangeli
womwe munamva, womwe unauzidwa m' kupanga konse
pansi pa mwamba; ndi womwe ine Paulos dinapangidwa
woimirira.
24 Tsopano disekera m' kumva kwanga kwa inu, ndimo
didzaza pa pande langa tshimene tshomwe tshirikupanda tsha
masautso a Kristu m' nyama yanga kwa tupi latshi, lomwe
25 liri eklesia; ndi lomwe dinapangidwa woimirira, kwa udindo
wa Mulungu womwe unapatsidwa kwa inu, ku dzaza mau a
26 Mulungu, *inde* kusadziwika komwe kunabisidwa kwa
magonero ndi kwa mafuko: koma tsopano tshasonyezedwa
27 kwa oyera atshi, kwa omwe Mulungu anasekera ku dziwitsa
zomwe ziri zolemera za kupambana kwa kusadziwika kumene
mwa Mitundu, komwe kuli Kristu mwa inu, kulingalira kwa
28 kupambana: emwe tiuza, kuambirira antu onse ndi ku-
punzitsa antu onse m' nzeru zonse, kuti tingopereka antu
29 onse akuta m' Kristu; kwa pomwe ditshita anso, kudzi-
fulumiza kwa kutshita kwatshi, komwe kutshita mwa ine
kolimba.

2 Kuti difuna inu ku dziwa bwanje kwakukuru didzifulumiza
kwa inu, ndi kwa awo pa Lawodikeya, ndi kwa ambiri
2 monga sanaona nkope yanga m' nyama; kuti mitima yao
ingosangalatsidwa, awo kugwirizanidwa m' kukonda, ndi
kwa zolemera zonse za kulimbitsa kodzaza kwa kudziwitsa,
3 kuti angodziwa kusadziwika kwa Mulungu, *inde* Kristu, mwa
emwe zolemera zonse za nzeru ndi kudziwa zibisidwa.
4 Dinena tshimene, kuti palibe modzi angonyenga inu ndi
5 kukantshizira kwa kunena. Kuti ngati diribe m' nyama,

kosuntira diripo ndi inu m' Nzimu, kusekera ndi kuona
kundandalika kwanu, ndi kulimbitsa kwa mvanu wanu m'
Kristu.

Ndimo monga munalandira Kristu Yesu Mwini, *tshointsho* 6
muenda mwa ie, osindidwa ndi omangidwa mwa ie, ndi 7
olimbitsidwa m' mvanu wanu, inde monga munapunzitsidwa,
kutshuruka m' kunena tshakonia.

Yang'anirani kani kudzakala modzi wina emwe apasula 8
inu mwa kukonda-nzeru kwatshi ndi tshinyengo tshatshabe,
pambuiu mwambi wa antu, pambuiu zoiamba za dziko,
ndimo si pambuiu Kristu: kuti mwa ie kukala kudzaza 9
konse kwa Umulungu kwatupi, ndimo mwa ie mudzazidwa, 10
emwe ali mutu wa ufumu wonse ndi mpamvu: mwa emwe 11
enso munadulidwa ndi kudula sikupangidwa ndi manja, m'
kubvula kwa tupi la nyama, m' kudula kwa Kristu;
kunaikidwa m' mwanda ndi ie m' mbapatisma, momwe 12
munaukitswa anso ndi ie mwa mvanu m' kutshita kwa
Mulungu, emwe anaukitsa ie kwa akufa. Ndimo inu, 13
munali akufa mwa matshimo anu ndi kusadula kwa nyama
yanu, inu, *dinena*, anafulumizana ndi ie, kunakululukiridwa
ife matshimo atu onse; kunafafanizidwa tshomangira tshole- 14
mbedwa m' mauzo tshomwe tshinali pa ife, tshomwe tshinali
pandunji pa ife: ndimo anatshitshotsa kwa njira, kukomera
itsho pa nkhwitshi; kunabvulidwa kwa ie eka maufumu ndi 15
zimpamvu, napanga kusonya kwa izo poyera, kupambana pa
izo mwa iko.

Ndimo palibe muntu aweruze inu ndi kudia, kapena 16
ndi kumwa, kapena ndi tshifukwa tsha siku lakudia,
kapena ndi mwezi watsopano kapena ndi dzua la
sabata: zomwe ziri tshitunzi tsha zintu zomwe zirinkudza; 17
koma tupi liri la Kristu. Palibe muntu alande inu kwa 18
sekeretso lanu ndi kusadzitama kofuna ndi kupembedza
kwa anjelo, kukala m' zintu zomwe waona, kutupitsidwa
kwatshabe ndi muwongo watshi wanyama, ndimo si 19
kugwiritsa Mutu, kwa womwe tupi lonse, kunakwanitsidwa
ndi kunagwiritsidwa mwa zinkonyo ndi zomangira, likula
ndi kukula kwa Mulungu.

Ngati munafa ndi Kristu kwa zoiamba za dziko, bwanje, 20
monga ngati kukala ndi moyo m' dziko, mudziika pansi pa
mauzo, Musagwira, kapena musalawa, kapena musatosa 21
(zintu zomwe zonse ziri ku mwaza ndi kutshita nazo), 22
pambuiu mau ndi mapunzitso a antu? Zintu zomwe 23

zipotshera nditu kusonya kwa nzeru m' kufuna-kupembedza,
ndi kusadzitama, ndi kulimba kwa tupi; *koma ziri* zopanda
ntengo pa kudzaza kwa nyama.

3 Ndimo ngati munaukitsidwa ndi Kristu, funani zintu zomwe
ziri za mwamba, pomwe Kristu ali, kukalitsidwa pa dzanja
2 lamanja la Mulungu. Ikani muwongo wanu pa zintu zomwe
3 ziri za mwamba, si pa zintu zomwe ziri pa dziko. Kuti
munafa, ndimo moyo wanu ubisidwa ndi Kristu mwa
4 Mulungu. Ntawi Kristu, *emwe ali* moyo watu, adzaso-
nyezedwa, pomwe inu unso ndi ie mudzasonyezedwa m'
kupambana.

5 Ndimo ipani dziwalo dzanu dzomwe dziri pa dziko;
dama, kusatsuka, kufunitsa, kufuna koipa, ndi kusirira,
6 komwe kuli kupembedza mafano; kwa zintu zomwe kufika
7 kukwiira kwa Mulungu pa ana a kusamvera; mwa zomwe
munaenda anso kali, ntawi munakala ndi moyo mwa zintu
8 zimenezi. Koma tsopano tshotsani inso zonse zimenezi;
kukwia, kukwiira, madano, kunyoza, kunena kwakumanyazi
9 mwa nkamwa mwanu: musanamizana; kuona kuti mwa-
10 bvula muntu wakali ndi ntshito zatshi, ndimo mwabvala
muntu watsopano, emwe alikufotokozedwa kwa kudziwa
11 pambuiu fanizo la ie emwe anapanga ie: pomwe kusadziwa
ku kala Mgrike ndi Myuda, kudula ndi kusadula, mbaribari,
Mskite, kapolo, mfulu: koma Kristu ali zonse, ndi mwa
zonse.

12 Ndimo bvalani, monga osang'kidwa a Mulungu, oyera
ndi okondedwa, ntima wa tshisoni, kukoma, kusadzitama,
13 kuyanja, kumva kutali; kulekerezana, ndi kukululukirana,
ngati muntu modzi apotshera tshulo pa wina; inde monga
14 Mwini anakululukira inu, tshointsho onso tshitani: ndimo
kopambana zintu zonse zimenezi *bvalani* kukonda, komwe
15 kuli tshomangira tsha kuta. Ndimo ntendere wa Kristu
ulekanitse m' mitima yanu, kwa womwe enso munaitanidwa
16 m' tupi limodzi; ndimo kalani oyamika. Mau a Kristu
akale mwa inu kolemera m' nzeru zonse; kupunzitsa ndi
kuambirirana ndi masalmo *ndi* zinyimbo *ndi* nyimbo
zanzimu, kuimba ndi kufatsa m' mitima yanu kwa Mulungu.
17 Ndimo tshomwe mutshita, m' mau kapena m' ntshito,
*tshitani* zonse m' dzina la Mwini Yesu, kunena tshakoma ku
Mulungu Atate mwa ie.

18 Akazi, kalani pansi pa amuna anu, monga kuli bwino
19 m' Mwini. Amuna, kondani akazi anu, ndimo musakala

okwia ndi awo. Ana, mverani atatu anu ndi amai anu m' 20
zintu zonse, kuti tshimene tshiri tshosekeretsa bwino m'
Mwini. Atate, musabvuta ana anu, kuti sadzatopetsedwa. 21
Akapolo, mverani m' zintu zonse awo omwe ali eni anu 22
kwa nyama; si ndi ntshito pa maso, monga osekeretsa-antu,
koma m' umodzi wa ntima, kuopa Mwini: tshomwe mutshita, 23
gwirani ntshito ndi ntima, monga kwa Mwini, ndimo si kwa
antu; kudziwa kuti kwa Mwini mudzalandira kulipira kwa 24
kuloa: muimirira Mwini Kristu. Kuti iemwe atshimwa 25
adzalandira anso kwa tshimo lomwe watshita: ndimo kulibe
tsang'ko. Eni, perekani kwa akapolo anu tshimene tshomwe 4
tshiri tshodeka ndi tshaumodzi; kudziwa kuti inu unso muli
ndi Mwini m' mwamba.

Mukalabe kolimbika m' pempero, kudikira momwe ndi 2
kunena tshakoma; ndi inso kupempera kwa ife enso,.kuti 3
Mulungu angotsegula kwa ife tshitseko kwa mau, ku la-
nkula kusadziwika kwa Kristu, kwa komwe diri inso m'
zomangira; kuti dingokusonyeza, monga dikanalankula. 4
Endani m' nzeru kwa awo omwe ali kunja, kuombola ntawi. 5
Kunena kwanu kukale ndi kufatsa ntawi zonse, kukometsedwa 6
ndi ntshere, kuti mungodziwa bwanje mukanaiang'ka onse.

Zintu zanga zonse Tikiko adzadziwitsa kwa inu, mbali 7
wokondedwa ndi woimirira wamvanu ndi kapolo nzanga m'
Mwini: emwe datumiza kwa inu kwa kuyerekeza kumene 8
nditu, kuti mungodziwa makalidwe atu, ndimo kuti
angosangalatsa mitima yanu; ndimo ndi Onesimo, mbali 9
wamvanu ndi wokondedwa, iemwe ali modzi wa inu.
Adzadziwitsa kwa inu zintu zonse zomwe *zitshitidwa* pano.

Aristarko womangidwa nzanga autsa inu, ndi Marko, 10
mwana wa mpwatshi wa amai atshi a Barnaba (ndi emwe
munalandira mau; ngati afika kwa inu, landirani ie), ndi 11
Yesu, emwe atshedwa Yusto, omwe ali a kudula: amene
oka *ali* otshita anz*anga* kwā dziko la Mulungu, antu omwe
mwakala kusangalatsa kwa ine. Epafra, emwe ali modzi wa 12
inu, kapolo wa Kristu Yesu, autsa inu, ntawi yonse
kudzifulumiza kwa inu m' mapempero atshi, kuti mungoima
akuta ndi olimbitsidwa kodzaza m' kufuna konse kwa
Mulungu. Kuti dimariza ie, kuti ali ndi ntshito yambiri 13
kwa inu, ndi kwa awo m' Lawodikeya, ndimo kwa awo m'
Yirapoli. Luka, sing'anga wokondedwa, ndi Dema autsa 14
inu. Utsani abali omwe ali m' Lawodikeya, ndi Nimfa, ndi 15
eklesia lomwe liri m' nyumba yao. Ndimo ntawi epistola 16

limene lawerengedwa mwa inu, werengetsani ilo inso ni'
eklesia la Alawodikeya; ndi kuti inu unso muwerenga
17 epistola kwa Lawodikeya. Ndimo nenani kwa Arkipo,
Tshenjera ndi kuimirira komwe walandira m' Mwini, kuti
ukudzaze.
18 Kuutsa kwa ine Paulos ndi dzanja langa loka. Kumbu-
kilani zomangira zanga. Kufatsa kukale ndi inu.

---

## EPISTOLA LATSHIMODZI LA PAULOS KWA

# ATESALONIKA.

1 PAULOS, ndi Silvano, ndi Timote, kwa eklesia la Atesa-
lonika m' Mulungu Atate ndi Mwini Yesu Kristu:
Kufatsa kwa inu ndi ntendere.
2 Tinena tshakoma kwa Mulungu kwa inu nonse ntawi
3 zonse, kutshula *ndi inu* m' mapempero atu; kukumbukila
kopanda kureka ntshito yanu ya mvanu ndi ntshito ya
kukonda ndi kulongosola kwa kulingalira m' Mwini watu
4 Yesu Kristu, patsogolo pa Mulungu watu ndi Atate; kudziwa,
5 abali okondedwa ndi Mulungu, kusang'kwa kwanu, tshifuka
kuti ivangeli watu usanafika kwa inu m' mau oka, koma
anso m' mpamvu, ndi m' Nzimu Woyera, ndimo *m'* kulimbi-
tsa-kudzaza kwakukuru; inde monga mudziwa makalidwe
6 anje a antu tinadzisonyeza ku inu kwa inu. Ndimo muna-
kala ofanizira a ife, ndi a Mwini, kunalandira mau m'
sautso yambiri, ndi tshimwemwe tsha Nzimu Woyera;
7 monga kuti munakala sonyezo kwa onse omwe amvana m'
8 Makedoniya ndi m' Akaya. Kuti kwa inu anabukitsa mau
a Mwini, si koka m' Makedoniya ndi Akaya, koma m' malo
onse mvanu wanu kwa Mulungu unaturuka; monga kuti
9 sitifuna ku lankula kantu. Kuti iwo oka abukitsa ndi ife
makalidwe anje a kuloa tinapotshera kwa inu; ndi bwanje
munatembenuka ku Mulungu kwa mafano, ku imirira
10 Mulungu wamoyo ndi woona, ndimo ku lindira kwa Mwana
watshi kwa kumwamba, emwe naukitsa kwa akufa, *inde*
Yesu, emwe atipulumutsa kwa kwiira kulinkudza.

Kuti inu noka, abali, mudziwa kuloa kwanu kwa inu, 2
kuti kusanapezedwa tshabe: koma kunamva patsogolo, ndimo 2
kunatshitidwa nai' koipa, monga mudziwa, pa Filipi, tina-
kula ndi kulimba ntima m' Mulungu watu ku lankula kwa
inu ivangeli wa Mulungu m' kumenyana kwambiri. Kuti 3
kutaulira kwatu si *kuli* kwa kutshimwa, kapena kwa kusa-
tsuka, kapena m' tshinyengo: koma inde monga tasimbidwa 4
ndi Mulungu kumvanidwa ndi ivangeli, tshointsho tilankula;
si monga kusekeretsa antu, koma Mulungu emwe ayesa
mitima yatu. Kuti kapena pa ntawi ina sitinapezedwa 5
kutshita ndi mau a kukometsera, monga mudziwa, kapena
tshopfundira tsha kusirira, Mulungu ali womariza; kapena 6
si kufuna kupambana kwa antu, kapena kwa inu, kapena
kwa ena, ntawi tinangokala olemerera, monga apostile a
Kristu. Koma tinali aulere pakati pa inu, monga ntawi 7
mulezi alera ana atshi: inde tshointsho, kuli kufuna kokonda 8
kwa inu, tinali osekera bwino ku patsa kwa inu, si ivangeli
wa Mulungu woka, koma anso mizimu yatu, tshifuka muna-
kala okondedwa nditu kwa ife. Kuti mukumbukila, abali, 9
ntshito yatu ndi kupwetekwa: kutshita usiku ndi usana,
kuti sitinangolemeretsa modzi wa inu, tinauza kwa inu
ivangeli wa Mulungu. Muli omariza, ndi Mulungu *unso*, 10
bwanje koyera ndi kodeka ndi kopanda tshulo tinadzitangata
kwa inu nomwe amvana: monga mudziwa bwanje *tinatshita* 11
*ndi* onse a inu, monga atate ndi ana atshi, kutaulira inu,
ndi kufulumiza *inu*, ndi kumariza, kwa nsonga kuti muka- 12
enda koenera kwa Mulungu, emwe aitana inu mwa dziko
latshi ndi kupambana.

Ndimo kwa tshifukwa tshimene ife enso tinena tshakoma 13
kwa Mulungu kopanda kureka, kuti, ntawi munalandira
kwa ife mau a kumva, *inde mau* a Mulungu, muna*a*landira si
*monga* mau a antu, koma, monga ali m' nteradi, mau a
Mulungu, omwe enso atshita mwa inu nomwe amvana. Kuti 14
inu, abali, munakala ofanizira a maeklesia a Mulungu omwe
ali m' Yudeya m' Kristu Yesu: kuti inu unso munamva
zintu zamodzi kwa omwe a fuko lanu, inde monga natshita a
Ayuda; omwe anapa Mwini Yesu ndi aprofeti, naturutsa 15
ife, ndimo osasekeretsa Mulungu, ndimo anali pandunji pa
antu onse; kuletsa ife ku lankula ndi Mitundu kuti ingo- 16
pulumutsidwa; kudzaza matshimo ao ntawi zonse: koma
kwiira kunafika pa awo kwa kutungo.

Koma ife, abali, kutshotsedwa kwa inu kwa nsiku 17

yeing'ono, ndi nkope, si ndi ntima, tinayerekeza kwambiri
kopambana ku ona nkope yanu ndi kufuna kwambiri:
18 tshifuka tinakafuna ku fika kwa inu, ine Paulos kamodzi
19 ndi inso; ndimo Satana natshedwetsa ife. Kuti kulingalira
kwatu kuli tshiani, kapena tshimwemwe, kapena tshisoti
tshotshuka tsha kupambana? Kodi simuli inu, patsogolo
20 pa Mwini watu Yesu pa kufika kwatshi? Kuti muli kupa-
mbana kwatu ndi tshimwemwe tshatu.

3 Mwa kuti ntawi sitinadziwa anso ku lekereza, tinaganiza
2 bwino ku siidwa pambuiu pa Atene oka; ndimo tinatumiza
Timote, mbali watu ndi woimirira wa Mulungu m' ivangeli
wa Kristu, ku limbikitsa inu, ndi ku sangalatsa *inu* ndi
3 mvanu wanu; kuti palibe muntu asuntidwa ndi masautso
amene; kuti inu noka mudziwa kuti kwa amene tiikidwa.
4 Kuti nditu, ntawi tinali ndi inu, tinauza inu kali kuti tiri
ku mva sautso; inde monga kunakala, ndimo mudziwa.
5 Kwa tshifukwa tshimene ine enso, ntawi sindinadziwa ku
lekereza ntawi ina, dinatumiza kuti dinangodziwa mvanu
wanu, kani ndi kantu wonyenga ananyenga inu, ndimo
6 ntshito yatu ikakala yatshabe. Koma ntawi Timote anafika
inde tsopano ku ife kwa inu, natenga kwa ife makalidwe
abwino a mvanu wanu ndi kukonda, ndi kuti muli ndi
kukumbukila kwabwino kwa ife ntawi yonse, kufunitsa
7 kutiona, inde monga ife enso *ku ona* inu; kwa tshifukwa
tshimene, abali, tinasangalatsidwa pa inu mwa tshisoni
8 tshatu tshonse ndi sautso mwa mvanu wanu: kuti tsopano
9 tiri ndi moyo, ngati muima kolimba m' Mwini. Kuti
kunena tshakoma kwanje tidziwa ku bweza anso kwa
Mulungu kwa inu, kwa tshimwemwe tshonse ndi tshomwe
10 tisekera kwa inu patsogolo pa Mulungu watu; usiku ndi
msana kupempera kwambiri kuti tingoona nkope yanu, ndi
tingotetsa tshomwe tshirikupanda mu mvanu wanu?
11 Ndimo Mulungu watu ndi Atate ie eka, ndi Mwini watu
12 Yesu, asonye njira yatu kwa inu: ndimo Mwini apange inu
ku kulitsa ndi ku tshurutsa m' kukonda modzi kwa wina,
ndi kwa antu onse, inde monga ife enso ti*tshita* kwa inu;
13 monga kuti angolimbikitsa mitima yanu yopanda tshulo m'
kuyera patsogolo pa Mulungu watu ndi Atate, pa kufika
kwa Mwini watu Yesu ndi oyera atshi onse.

4 Ndimo kwakutungo, abali, tipempa ntitaulira inu m' Mwini
Yesu, kuti, monga munalandira kwa ife bwanje mukanaenda
ndi mukanasekeretsa Mulungu, inde monga muenda,—kuti

mutshurutse koyenjezerayenjezera. Kuti mudziwa mauzo 2
anje tinapatsa inu mwa Mwini Yesu. Kuti kumene kuli 3
kufuna kwa Mulungu, *inde* kuyeretsa kwanu, kuti muleka
kwa dama; kuti onse a inu adziwa bwanje kudzipotshera 4
ndi tshiwira tshatshi m' kuyeretsa ndi ulemu, si m' kufu- 5
nitsa kwa kufuna, inde monga Mitundu yomwe yosadziwa
Mulungu; kuti palibe muntu atshenjerera, natshimwa ndi 6
mbali watshi m' tshintu: tshifuka Mwini ali wozimbula m'
zintu zonse zimenezi, monga anso ife tinatshenjeza inu kali
ntinamariza. Kuti Mulungu sanaitana ife kwa kusatsuka, 7
koma m' kuyeretsa. Ndimo ie emwe ataia, wosataia muntu, 8
koma Mulungu, emwe apatsa Nzimu Woyera watshi kwa inu.
Koma ndi kukonda kwa abali musakala ndi uko kuti 9
modzi alemba kwa inu: kuti inu noka mupunzitsidwa ndi
Mulungu ku kondana; kuti nditu mukutshita kwa abali 10
onse omwe ali m' Makedoniya lonse. Koma titaulira inu,
abali, kuti mutshurutse kuyenjezerayenjezera; ndi kuti 11
muyerekeze ku kala otshete, ndimo ku tshita ntshito yanu,
ndimo ku tshita ndi manja anu, inde monga tinauza inu;
kuti mungoenda kwaulemu kwa awo omwe ali kunja, 12
ndimo mungofunira palibe kantu.
Koma sitifuna inu ku kala opulukira, abali, ndi awo 13
omwe agona; kuti musakala ndi tshisoni, inde monga
otsala, omwe osapotshera kulingalira. Kuti ngati timvana 14
kuti Yesu anafa ndimo nauka anso, inde tshointshi awa
anso omwe anagona m' Yesu Mulungu adzatenga ndi ie.
Kuti tinena tshimene kwa inu ndi mau a Mwini, kuti ife tomwe 15
tiri amoyo, tomwe tisiidwa kwa kufika kwa Mwini, sitidzapita
patsogolo pa awo omwe anagona. Kuti Mwini ie eka adzatsika 16
kwa kumwamba, ndi kupfula, ndi liu la njelo-wang'kuru,
ndimo ndi lipenga la Mulungu: ndimo akufa m' Kristu adza-
uka poiamba: pomwe ife tomwe tiri amoyo, tomwe tisiidwa, 17
tidzakwatulidwa nao m' mitambo, ku komana ndi Mwini m'
mlengalenga: ndimo tshointsho tidzakala ntawi yonse ndi
Mwini. Mwa kuti sangalatsanani ndi mau amene. 18
Koma ndi zintawi ndi zinsiku, abali, musali ndi uko kuti 5
kantu kalembedwa kwa inu. Kuti inu noka mudziwa kota kuti 2
siku la Mwini tshointsho lifika monga woba musiku. Ntawi 3
alikunena, Ntendere ndi kupulumuka, pomwe kumwaza kwa-
nsangu ku fika pa awo, monga kupwetekwa pa nkazi ndi
mwana; ndimo osadziwa nditu ku pulumuka. Koma inu, 4
abali, simuli mundima, kuti siku limene likafikiriza inu monga

5 woba: kuti inu nonse muli ana a kuunika, ndi ana a
6 msana: ife sitiri a usiku, kapena a ndima; ndimo tsho-
intshi leka ife sikugona, monga otsala, koma lekani ife ku
7 dikira ndimo ku kala kosaledzera. Kuti awo omwe agona
tulo agona tulo usiku; ndimo awo omwe ali oledzera ali
8 oledzera usiku. Koma lekani ife, monga tiri a msana,
ku kala kosaledzera, kubvala mtshinjirizo wa mvanu ndi
kukonda; ndi kwa tshisoti, kulingalira kwa kupulumutsa.
9 Kuti Mulungu naikidwa ife si kwa kukwiira, koma kwa
kulandira kwa kupulumutsa mwa Mwini watu Yesu Kristu,
10 emwe anafera kwa ife, kuti, kapena tiri maso kapena
11 tigona, tikakala ndi ie. Mwa kuti tauliranani, ndi manga-
nani, inde monga anso mutshita.
12 Koma tipempa inu, abali, ku dziwa awo omwe agwira
ntshito mwa inu, ndimo ali pamwamba pa inu m' Mwini,
13 naambirira inu, ndimo ku ganikiza awo kwambiri kopambana
m' kukonda kwa ntshito yao. Kalani ndi ntendere mwa
14 inu noka. Ndimo titaulira inu, abali, ambirirani atshiwawa,
fulumizani ofokamitima, tshirikizani ofoka, imvani kwa-
15 kutali kwa onse. Yang'anirani kuti palibe modzi abweza
ku modzi mpulupulu kwa mpulupulu; koma ntawi zonse
tsatani tshimene tshomwe tshiri tshabwino, modzi kwa wina,
16.17 ndi kwa onse. Sekerani ntawi yonse; pemperani kopanda ku
18 leka; m' zintu zonse nenani tshakoma: kuti tshimene tshiri
19 kufuna kwa Mulungu m' Kristu Yesu kwa inu. Musa-
20.21 zima Nzimu; musanyoza maloso; yesani zintu zonse;
22 gwirani kolimba tshimene tshomwe tshiri tshabwino; lekani
makalidwe onse a mpulupulu.
23 Ndimo Mulungu wa ntendere ie eka ayeretse inu kota;
ndimo nzimu wanu ndi moyo ndi tupi zingosungidwa zota,
zopanda tshulo pa kufika kwa Mwini watu Yesu Kristu.
24 Wamvanu ali ie emwe aitana inu, emwe enso adzakutshita.
25 Abali, pemperani kwa ife.
26.27 Utsani abali onse ndi kumsomsona koyera. Dilimbikitsa
inu ndi Mwini kuti epistola limene liwerengedwa kwa abali
onse.
28 Kufatsa kwa Mwini watu Yesu Kristu kukale ndi inu.

## EPISTOLA LATSHIWIRI LA PAULOS KWA

# ATESALONIKA.

PAULOS, ndi Silvano, ndi Timote, kwa eklesia la Atesa- 1
lonika m' Mulungu Atatu atu ndi Mwini Yesu
Kristu: Kufatsa kwa inu ndi ntendere kwa Mulungu Atate 2
ndi Mwini Yesu Kristu.

Tifulumizidwa ku patsa tshakoma ku Mulungu ntawi 3
zonse kwa inu, abali, inde monga tshiri tshabwino, tshifuka
kuti mvanu wanu ukula kwambiri, ndi kukondana kwa inu
nonse kutshurukitsa; tshointsho kuti ife toka tipambana 4
mwa inu m' maeklesia a Mulungu kwa kulongosola kwanu
ndi mvanu m' mazunzo anu onse ndi m' masautso omwe
mumvabe; *tshomwe tshiri* tshizindikilo tshosonyezedwa tsha 5
kuweruza kodeka kwa Mulungu; kwa nsonga kuti mu-
ngowerengedwa oenera a dziko la Mulungu, kwa lomwe
inu unso mumva: ngati kuli tshointsho kuti tshiri tshintu 6
tshodeka ndi Mulungu ku lipira sautso kwa awo omwe
asautsa inu, ndimo kwa inu omwe asautsidwa kupuma ndi 7
ife pa kusonyeza kwa Mwini Yesu kwa kumwamba ndi
anjelo a mpamvu yatshi m' malilume a moto, ku pereka 8
kuzimbula kwa awo omwe osadziwa Mulungu, ndi kwa awo
omwe osamvera ivangeli wa Mwini watu Yesu: omwe 9
adzamva kulanga, *inde* kumwaza kosamariza kwa nkope ya
Mwini ndi kwa kupambana kwa kulimba kwatshi, ntawi 10
adzafika ku pambanitsidwa m' oyera atshi, ndimo ku zi-
zwitswa nai' m' awo onse omwe anamvana (tshifuka kumariza
kwatu kwa inu kunamvanidwa) m' siku limene. Ku nsonga 11
yomwe ife enso tipempera kwa inu ntawi yonse, kuti
Mulungu watu angowerenga inu oenera a kuitana kwanu,
nangodzaza kufuna konse kwa ubwino ndi ntshito *zonse*
za mvanu, ndi mpamvu; kuti dzina la Mwini watu Yesu 12
lingopambanitsidwa mwa inu, ndimo inu mwa ie, kwa
kufatsa kwa Mulungu watu ndi Mwini Yesu Kristu.

Ndimo tipempa inu, abali, kwa kufika kwa Mwini watu 2
Yesu Kristu, ndi kusong'kana kwatu kwa ie; kwa nsonga 2
kuti musagwedezedwa nsanga kwa muwongo wanu, kapena

kosuntira musantuntumiridwa, kapena ndi nzimu, kapena
ndi mau, kapena ndi epistola monga kwa ife, monga kuti
3 siku la Mwini liripo; palibe muntu anyenge inu m' kantu:
kuti *losadzakala*, kani kuleka kufika poiamba, ndi muntu wa
4 mpulupulu asonyezedwa, mwana wa kumwazika, iemwe
adzikana ndi adzitalikitsa pa onse omwe atshedwa Mulungu
kapena omwe apembedzedwa; monga kuti akala m' malo
5 oyera a Mulungu, kudzisonyeza monga Mulungu. Kodi
musakumbukila, kuti, ntawi dinali kosuntira ndi inu,
6 dinauza inu zintu zimenezi? Ndimo tsopano mudziwa
tshimene tshomwe tshiimitsa, kwa nsonga kuti angosonye-
7 zedwa m' nsiku yatshi. Kuti kusadziwika kwa kusamvera-
mau kutshita kali: koka *kuli* modzi emwe aimitsa tsopano,
8 kwa ntawi atshotsedwa kwa njira. Ndimo pomwe adza-
sonyezedwa wakusamvera-mau, emwe Mwini Yesu adzapa
ndi pwea la nkamwa mwatshi, ndimo adzatenga kwa tshabe
9 ndi kusonyeza kwa kufika kwatshi; *inde ie* kufika kwa
emwe kuli kwa kutshita kwa Satana ndi mpamvu yonse ndi
10 zizindikilo ndi zozizwa zonama, ndimo ndi tshinyengo
tshonse tsha kusadeka kwa awo omwe alikumwazika;
tshifuka sanalandira kukonda kwa nteradi, kuti anango-
11 pulumutsidwa. Ndimo kwa tshifukwa tshimene Mulungu
atumiza awo kutshita kwa tshimo, kuti akamvana bodza:
12 kuti awo onse anangoweruzidwa omwe osamvana nteradi,
koma nakala ndi kusekera m' kusadeka.

13 Koma tifulumizidwa ku nena tshakoma kwa Mulungu
ntawi yonse kwa inu, abali okondedwa ndi Mwini, tshifuka
kuti Mulungu anasang'ka inu kwa kuamba kwa kupulu-
14 mutsa m' kuyeretsa kwa Nzimu ndi mvanu wa nteradi: kwa
komwe naitana inu mwa ivangeli watu, kwa kulandira kwa
15 kupambana kwa Mwini watu Yesu Kristu. Ndimo tsho-
intsho, abali, imani kolimba, ndimo gwiritsani miambi yomwe
munapunzitsidwa, kapena ndi mau, kapena ndi epistola
latu.

16 Ndimo Mwini watu Yesu Kristu ie eka, ndi Mulungu
Atatu atu emwe nakonda ife napatsa ife kusangalatsa kosa-
17 mariza ndi kulingalira kwabwino mwa kufatsa, asangalatse
mitima yanu ndimo alimbitse iyo m' ntshito zonse zabwino
ndi mau.

3 Kwakutungo, abali, pemperani kwa ife, kuti mau a
Mwini angotamanga nangopambanitsidwa, inde monga
2 anso *ali* ndi inu; ndimo kuti tingopulumutsidwa kwa antu

opanda nzeru ndi oipa; kuti onse osapotshera mvanu.
Koma Mwini ali wamvanu, emwe adzalimbitsa inu, nadza- 3
dikira inu kwa *wa*mpulupulu. Ndimo tiri ndi kumvana 4
m' Mwini ndi inu, kuti mutshita ndimo mudzatshita zintu
zomwe tiuza. Ndimo Mwini asonya mitima yanu m' ku- 5
konda kwa Mulungu, ndi m' kulongosola kwa Kristu.

Ndimo tiuza inu, abali, m' dzina la Mwini watu Yesu 6
Kristu, kuti mubwerera inu noka kwa abali onse omwe aenda
kwatshiwawa, ndimo si pambuiu pa mwambi womwe anala-
ndira kwa ife. Kuti inu noka mudziwa bwanje mukanafa- 7
nizira ife: kuti sitinadzitangata kwatshiwawa mwa inu; 8
kapena sitinadia nkate kwa tshabe pa dzanja la muntu modzi,
koma m' ntshito ndi kupwetekwa, kutshita usiku ndi msana,
kuti sitinangolemetsa modzi wa inu: si tshifuka sitipotshera 9
kwatu, koma kudzipanga sonyezo kwa inu, kuti mukanafa-
nizira ife. Kuti inde ntawi tinali ndi inu, tinauza inu tshi- 10
mene, Ngati modzi wosafuna ku tshita, kapena asadie. Kuti 11
timva ndi ena omwe aenda mwa inu kwatshiwawa, omwe
osatshita konse, koma ali zitserekwete. Ndimo omwe ali otere 12
tiuza ndimo titaulira m' Mwini Yesu Kristu, kuti ndi kuto-
ntola atshita, nadia nkate wao. Koma inu, abali, musalema 13
m' kutshita bwino. Ndimo ngati muntu modzi wosamvera 14
mau atu ndi epistola limene, yang'anira muntu amene, kuti
musakala nai', kwa nsonga kuti angokala ndi manyazi.
Ndimo *kosuntira* musawerenga ie monga liwongo, koma 15
ambirirani ie monga mbali.

Ndimo Mwini wa ntendere ie eka apatse inu ntendere 16
pa ntawi zonse m' njira zonse. Mwini akale ndi inu nonse.

Kuutsa kwa ine Paulos ndi dzanja langa loka, lomwe liri 17
tshizindikilo m' maepistola onse: tshointsho dilemba.
Kufatsa kwa Mwini watu Yesu Kristu kukale ndi inu 18
nonse.

## EPISTOLA LATSHIMODZI LA PAULOS KWA

# TIMOTE.

1 PAULOS, mpostile wa Kristu Yesu kwa mau a Mulungu
Mpulumutsi watu, ndimo Kristu Yesu kulingalira
2 kwatu; kwa Timote, mwana wanga woona m' mvanu:
Kufatsa, nsisi, ntendere, kwa Mulungu Atate ndi Kristu
Yesu Mwini watu.
3 Monga dinataulira iwe ku kala pa Feso, ntawi dinalikuloa
m' Makedoniya, kuti unangouza antu ena sikupunzitsa
4 kupunzitsa kwina, kapena sikusamala ndi zintanu ndi
mafuko opanda-nsonga, zomwe ziturutsa mafunso, kopa-
mbana udindo wa Mulungu womwe uli m' mvanu; *tsho-*
5 *intsho ditshita tsopano.* Koma nsonga ya kuuza iri kukonda
kwa ntima woyera ndi kudzidziwitsa kwabwino ndi mvanu
6 wosanyengedwa: kwa zintu zomwe ena analembetuka mwa-
7 tembenuka kwa kulankula kwautsiru; kufuna ku kala
apunzitsi a mau, ngati osadziwa kapena tshomwe anena,
8 kapena ndi tshomwe atshimika. Koma tidziwa kuti mau
ali abwino, ngati muntu atshita nao kwamau, monga kudzi-
9 wa kumene, kuti mau osapangidwa kwa muntu wodeka,
koma kwa osamvera mau ndi osaweruzika, kwa osapembedza
ndi ampulupulu, kwa osayera ndi anko, kwa ambanda a
10 atate ndi ambanda a amai, kwa ambanda, kwa otshita dama,
kwa akuyeruka, kwa olanda a antu, kwa onama, kwa osi-
njirira, ndimo ngati kalipo kantu kena pandunji pa ku-
11 punzitsa kolimbika; kwa ivangeli wa kupambana kwa
Mulungu wodala, womwe unaperekedwa kwa kumvana
kwanga.
12 Dinena tshakoma kwa ie emwe analimbitsa ine, *inde*
Kristu Yesu Mwini watu, tshifuka kuti naganiza ine wa-
13 mvanu, kuika ine kwa kuimirira *kwatshi;* ngati kali dinali
wotukwana, ndi wozunza, ndi wopweteketsa: koma dinala-
ndira nsisi, tshifuka dinatshitshita kopulukira m' kusa-
14 mvana; ndimo kufatsa kwa Mwini watu kunatshuruka kwa-
mbiri ndi mvanu ndi kukonda komwe kuli m' Kristu Yesu.
15 Amvanu ali mau, ndi oenera a kulandira konse, kuti Kristu
Yesu nafika m' dziko ku pulumutsa ampulupulu; wa omwe
16 diri wopambana: koma kwa tshifukwa tshimene dinalandira

nsisi, kuti mwa ine monga wopambana Yesu Kristu anango-
sonyeza kumva kutali kwatshi konse, kwa sonyezo kwa awo
omwe akamvana ndi ie pambuiu ku moyo wosamariza.
Ndimo kwa Fumu Yotshuka ya magonero, yosabvunda, 17
yosaonekedwa, Mulungu eka, *zikale* ulemu ndi kupambana
kwa magonero a magonero. Amen.

Kuuza kumene diika pa iwe, mwana wanga Timote, kwa 18
maloso omwe napita patsogolo pa iwe, kuti ndi awo ungo-
panga nkondo m' nkondo yabwino; kukala ndi mvanu ndi 19
kudzidziwitsa kwabwino; komwe ena anakang'ka kwa awo
nabandula ndi mvanu: a omwe ali Himenayo ndi Alesandire; 20
omwe dinapereka kwa Satana, kuti anangopunzitsidwa si ku
tukwana.

Ndimo ditaulira, patsogolo pa onse, kuti mapempo, ma- 2
pempero, maletsetso, maamiko, apangidwa kwa antu onse;
kwa mafumu otshuka ndi onse omwe ali m' malo otalika; 2
kuti tingokala ndi moyo wantendere ndi watshete m' kupe-
mbedza konse ndi upe. Tshimene tshiri tshabwino ndi 3
tsholandiridwa m' kuona kwa Mulungu Mpulumutsi watu;
emwe afuna kuti antu onse akapulumutsidwa, ndimo akafika 4
kwa kudziwa kwa nteradi. Kuti alipo Mulungu modzi, ndi 5
wolekanitsa modzi pakati pa Mulungu ndi antu, *ie eka* muntu,
Kristu Yesu, emwe anapatsa ie eka dombolo kwa onse; 6
kumariza *ku nyamulidwa* m' ntawi zatshi; kwa komwe 7
dinaikidwa wouza ndi mpostile (dinena nteradi, sindinama),
mpunzitsi wa Mitundu m' mvanu ndi nteradi.

Ndimo difuna kuti amuna apempera m' malo onse, kutu- 8
kula manja oyera, opanda kukwiira ndi kukang'gana.
Modzimodzi, kuti akazi adzibvale nsaru zosaopsa ndi ma- 9
nyazi ndi kudziweruza; si ndi tsisi louluka, ndi golide
kapena maperile kapena miinjiro ya ntengo wapatali; koma 10
(komwe kukalitsa bwino akazi kubvomereza kupembedza)
mwa ntshito zabwino. Nkazi apunzire m' kutontola ndi 11
kukala pansi konse. Koma sindilola nkazi ku punzitsa, 12
kapena ku kala ndi kuweruza pa mamuna, koma ku kala
m' kutontola. Kuti Adam anapangidwa poiamba, Heva 13
pambuiu; ndimo Adam sananyengedwa, koma nkazi kuna- 14
nyengedwa wagwa m' tshimo: koma adzapulumutsidwa 15
mwa kubala mwana, ngati akalabe mumvanu ndi kukonda
ndi kuyeretsedwa ndi kudziweruza.

Kwamvanu kuli kunena, Ngati muntu afuna untshito 3
wa woyang'anira, afuna ntshito yabwino. Ndimo woyang'- 2

anira akanakala wopanda sinjiriro, mamuna wa nkazi modzi,
wosaledzera, wodziweruza, wabwino, wosungira alendo,
3 wanzeru ku punzitsa; si wolongolola, si womenya; koma
4 waulere, si wandeu, si wokonda wa ndrama; modzi emwe
aweruza bwino nyumba yatshi, kuli ndi ana *atshi* pansi pa
5 *ie* ndi upe wonse; (koma ngati muntu wosadziwa bwanje ku
weruza nyumba yatshi, adziwa bwanje ku sungira eklesia la
6 Mulungu?) si woiambira, kani kutupitsidwa agwa m'
7 kuweruza kwa diabolos. Ndimo akanapotshera kumariza
kwabwino kwa awo omwe ali kunja; kani agwa m' sinjiriro
8 ndi khwekwe za diabolos. Oimirira modzimodzi *akanakala*
ape, si a malilume awiri, si kumwetsa vinyo ambiri, si
9 oumira a ndrama zonyansa; kugwira kusadziwika kwa
10 mvanu m' kudzidziwitsa koyera. Ndimo amene enso
poiamba ayesedwe; pomwe aimirire monga oimirira, ngati
11 ali opanda tshulo. Akazi modzimodzi *akanakala* ape, si
12 anseke, osaledzera, amvanu m' zintu zonse. Oimirira akale
amuna a nkazi modzi, kuweruza ana *ao* ndi nyumba zao
13 zabwino. Kuti awo omwe anaimirira bwino monga oimirira
alandira kwa awo oka kuima kwabwino, ndi kulimbika
kwakukuru m' mvanu womwe uli m' Kristu Yesu.
14 Zintu zimenezi dilemba kwa iwe, kulingalira ku fika kwa
15 iwe m' ntawi yeing'ono; koma ngati dikala ntawi yeitali, kuti
ungodziwa bwanje antu akanadzitangata m' nyumba ya
Mulungu, yomwe iri eklesia la Mulungu wamoyo, nzati ndi
16 kuzika za nteradi. Ndimo kopanda kukang'gana kwakukuru
kuli kusadziwika kwa kupembedza; Ie emwe anasonyezedwa
m' nyama, anadeketsedwa m' nzimu, anaonedwa ndi anjelo,
anauzidwa mwa mitundu, anamvanidwa m' dziko, analandi-
ridwa m' kupambana.
4 Koma Nzimu uti poyera, kuti m' ntawi zapambuiu ena
adzagwa kwa mvanu, kusamala ndi mizimu yotshimwitsa
2 ndi mapunzitso a ademon, mwa kunyenga kwa antu omwe
anena mabodza, naotshedwa m' kudzidziwitsa kwao monga
3 ndi tshitsulo tshotenta; kuletsa ku kwata, *ndi kuuza* ku leka
zakudia, zomwe Mulungu anazipanga ku landiridwa ndi
kunena tshakoma ndi awo omwe amvana nadziwa nteradi.
4 Kuti zopangidwa zonse za Mulungu ziri zabwino, ndimo
palibe kantu kuli ku taiidwa, ngati kulandiridwa ndi kunena
5 tshakoma: kuti kuyeretsedwa mwa mau a Mulungu ndi
mpempero.
6 Ngati ukumbutsa abali ndi zintu zimenezi, udzakala

woimirira wabwino wa Kristu Yesu, unaleredwa m' mau a
mvanu, ndi a kupunzitsa kwabwino komwe watsata *kwa*
*ntawi ya tsopano*: koma kana ntanu zanko ndi za akazi 7
ankalamba. Ndimo udzitshita kwa kupembedza: kuti 8
kudzitshita kwatupi kupindulidwa kang'ono; koma kupe-
mbedza kupindulidwa kwa zintu zonse, kuli ndi lonjezano la
moyo womwe uli tsopano, ndimo wa umene womwe uli ku
fika. Kwamvanu kuli kunena, ndi koenera ndi kula- 9
ndira konse. Kuti kwa nsonga imene titshita ndimo 10
tidzifulumiza, tshifuka taika kulingalira kwatu pa Mulungu
wamoyo, emwe ali Mpulumutsi wa antu onse, kopambana
kwa awo omwe amvana. Zintu zimenezi uuza nupunzitsa. 11
Palibe muntu anyoze unyamata wako; koma kala sonyezo 12
ku awo omwe amvana, m' mau, m' makalidwe a moyo, m'
kukonda, m' mvanu, m' kuyera. Kwa ntawi difika, samala 13
kuwerenga, kutaulira, kupunzitsa. Usaononga ntulo womwe 14
uli mwa iwe, womwe unapatsidwa kwa iwe ndi kulosa, ndi
kuika kwa manja a gulu la akuru. Kala ndi tshangu m' 15
zintu zimenezi; patsa iwe eka kota kwa izo; kuti kupitirira
kwako kungosonyezedwa kwa onse.

Tshenjera kwa iwe eka, ndi kwa kupunzitsa kwako. 16
Kalabe m' zintu zimenezi; kuti m' kutshita kumene udza-
pulumutsa iwe eka ndi awo omwe amva iwe.

Usasulumula mkuru, koma taulira ie monga atate; 5
ang'ono monga abali: akazi akuru monga amai; ang'ono 2
monga alongo, m' kuyera konse. Lemekeza amasie omwe 3
ali amasie nditu. Koma ngati wamasie modzi ali ndi ana 4
kapena ana a ana, apunzire poiamba ku sonya kupembedza
kwa fuko lao, ndi ku bwezera atatu ao ndi amai ao: kuti
tshimene tshiri tsholandiridwa m' kuona kwa Mulungu.
Koma ie emwe ali wamasie nditu, ndi wadzinja, waika 5
kulingalira kwatshi pa Mulungu, ndimo akalabe ndi
mapempo ndi mapempero usiku ndi msana. Koma ie emwe 6
adzipatsa kwa kusekera ali wakufa ntawi ali ndi moyo.
Zintu zimenezi inso uza, kuti angokala opanda sinjiriro. 7
Koma ngati modzi wosakwanitsira kwa kwatshi, ndi kopa- 8
mbana kwa banja latshi, wakana mvanu, ndimo ali woipa
wopambana wosamvana. Palibe modzi alembedwe monga 9
wamasie pansi pa dzaka makumi asanu ndi modzi, *anakala*
nkazi wa muntu modzi, wabukitsidwa bwino kwa ntshito 10
zabwino; ngati walera ana, ngati wasungira alendo, ngati
watsuka mapazi a oyera, ngati wapeputsa osautsidwa, ngati

11 watsata kwatshangu ntshito zonse zabwino. Koma amasie
ang'ono ukana: kuti ntawi anakula onyoza pa Kristu, afuna
12 ku kwatibwa; ali ndi sutso, tshifuka anataia mvanu wao
13 woiamba. Koma pamodzi apunzira anso *ku kala* olesi,
kuendaenda kwa nyumba ndi nyumba; ndimo si olesi koka,
koma olongololo onso ndi zitserekwete, kulankula zintu
14 zomwe sakana*lankula*. Ndimo difuna kuti *amasie* ang'ono
akwatibwe, abale ana, aweruze banja, osapatse tshifukwa
15 kwa liwongo kwa kunyoza: kuti kali ena atembenuzidwa
16 pambuiu Satana. Ngati nkazi modzi emwe amvana ali ndi
amasie, apeputse awo, ndimo eklesia lisalemedwe; kuti
lingopeputsa awo omwe ali amasie nditu.
17 Akuru omwe aweruza bwino aganizidwe oenera a ulemu
wopindidwa, kopambana awo omwe atshita m' mau ndi
18 kupunzitsa. Kuti lemba liti, Usapunamiza ng'ombe ntawi
ikulunga dzintu. Ndimo, Wotshita ali woenera wa kulipira
19 kwatshi. Pa mkuru usalandira tshulo, kani pa *nkamwa*
20 *mwa* omariza awiri kapena atatu. Awo omwe atshimwa
sulumula m' kuona kwa onse, kuti otsala anso angokala m'
21 kuopa. Diuza *iwe* m' kuona kwa Mulungu, ndi Kristu
Yesu, ndi anjelo osang'kidwa, kuti usungira zintu zimenezi
22 wopanda kusang'ka, kusatshita kantu ndi kuanja. Usaika
manja kwansangu pa muntu modzi, kapena usakala wogawa
wa mpulupulu za antu ena: sungira iwe eka woyera.
23 Usakala ntawi ina womwa madzi, koma tshita ndi vinyo
wang'ono kwa tshipfu tshako ndi kwa zofoka zako ntawi
24 zambiri. Mpulupulu za antu ena ziri zoonedwa, zipita
patsogolo pa kuweruza; ndimo antu ena anso zitsata.
25 Modzimodzi inso ziri ntshito zabwino zomwe zionedwa;
ndimo zotere monga ziri zina zosadziwa ku bisidwa.
6 Monga ambiri monga ali akapolo pansi pa tshigologolo
aganize ambuiye ao oenera a ulemu wonse, kuti dzina la
2 Mulungu ndi kupunzitsa sizitukwanidwa. Ndimo awo
omwe apotshera ambuiye omvana, sianyoze awo, tshifuka ali
abali; koma aimirire awo kopambana, tshifuka awo omwe
agawana ndi kutshita kwabwino ali omvana ndimo ali
okondedwa. Zintu zimenezi punzitsa ndi taulira.
3 Ngati muntu modzi apunzitsa kupunzitsa kwina, ndimo
wosabvomera ku mau olimba, *inde* mau a Mwini watu
Yesu Kristu, ndi kwa kupunzitsa komwe kuli kwa kupe-
4 mbedza; ali wotupitswa, kudziwa palibe kantu, koma
kufoka ndi mafunso ndi makang'gano a mau, kwa omwe zifika

dano, ndeu, manyozo, matshenjero oipa, malongololo a antu 5
obvunda m' muwongo natshotsedwa kwa nteradi, kuganiza-
ganiza kuti kupembedza kuli njira ya kupindula. Koma 6
kupembedza ndi kusanyanyala kuli kupindula kwakukuru:
kuti tinatenga palibe kantu m' dziko, kuti kapena tidziwa ku 7
turutsa palibe kantu; koma kuli ndi kudia ndi kupfundira ndi 8
zimenezi sitidzanyanyala. Koma awo omwe afuna ku kala 9
olemera agwa m' tshinyengo ndi m' khwekwe ndi mafuno
ambiri opusa ndi opwetekesa, otere monga abiritsa antu m'
kuononga ndi kumwaza. Kuti kukonda kwa ndrama kuli 10
ntsitsi wa mitundu yonse ya mpulupulu: komwe ena
kuyesera pambuiu anasotsheretsedwa kwa mvanu, ndimo
nadzibola ndi zisoni zambiri.

Koma iwe, O muntu wa Mulungu, tawa zintu zimenezi; 11
nutsata kudeka, kupembedza, mvanu, kukonda, kulongosola,
kuanja. Menyana kumenyana kwabwino kwa mvanu, 12
gwiritsa pa moyo wosamariza, kwa zomwe unaitanidwa,
ndimo unabvomereza kubvomereza kwabwino m' kuona
kwa omariza ambiri. Diuza iwe m' kuona kwa Mulungu, 13
emwe afulumiza zintu zonse, ndi kwa Kristu Yesu, emwe
patsogolo Pontiyo Pilato anamariza kubvomereza kwabwino;
kuti usunge mau, opanda banga, opanda sinjiriro, kwa 14
kuonekera kwa Mwini watu Yesu Kristu: komwe m' ntawi 15
zatshi adzasonyeza, emwe ali Wampamvu wodala ndi eka,
Fumu Yotshuka ya mafumu otshuka, ndi Mwini wa eni;
emwe eka ali ndi kusafa, kukala m' kuunika kusafikidwa; 16
emwe palibe muntu waona, kapena adziwa ku ona: kwa
emwe *zikale* ulemu ndi mpamvu zosamariza. Amen.

Uza awo omwe ali ndi zolemera m' kugonera kumene 17
kwatsopano, kuti osakala muwongo-mudzitama, kapena
osapotshera kulingalira kwao kuikidwa pa kusadziwa kwa
zolemera, koma pa Mulungu, emwe apatsa ife kolemera
zintu zonse ku sekera; kuti atshite bwino, kuti alemere ndi 18
ntshito zabwino, kuti akale akuta ku gawaniza, kufuna ku
mva tshisoni ndi ena; kuika m' nkokwe kwa awo oka 19
kuzika kwabwino pa ntawi iri kufika, kuti angogwira pa
moyo womwe uli *moyo* nditu.

O Timote, dikira kuikirira, kutembenuka kwa malongololo 20
anko ndi makano za kudziwa komwe kutshedwa tshointsho
konama; komwe ena kubvomera wapita kwa mvanu. 21

Kufatsa kukale ndi inu.

EPISTOLA LATSHIWIRI LA PAULOS KWA

# TIMOTE.

1 PAULOS, mpostile wa Kristu Yesu mwa kufuna kwa
Mulungu, kwa lonjezano la moyo womwe uli m'
2 Kristu Yesu, kwa Timote, mwana wokondedwa wanga:
Kufatsa, nsisi, ntendere, kwa Mulungu Atate ndi Kristu
Yesu Mwini watu.
3 Dinena tshakoma kwa Mulungu, emwe diimirira kwa
atate akali anga m' kudzidziwitsa koyera, bwanje
kosareka kuli kukumbukila kwanga kwa iwe m' mapempo
4 anga, usiku ndi msana kufunitsa ku ona iwe, kukumbukila
5 misozi yako, kuti dingodzazidwa ndi tshimwemwe; kunaku-
mbutsidwa kwa mvanu wosanyenga womwe uli mwa iwe;
womwe unakala poiamba m' amai ako akuru Loyis, ndi
amai ako Yunike; ndimo, dikantshiziridwa, mwa iwe enso.
6 Kwa tshifukwa tshomwe dikumbutsa iwe kuti ufulumize
ntulo wa Mulungu, womwe uli mwa iwe mwa kuika kwa
7 manja anga. Kuti Mulungu sanatipatsa nzimu wa kuopa;
8 koma wa mpamvu ndi kukonda ndi kudziweruza. Ndimo
usakala ndi manyazi ndi kumariza kwa Mwini watu, kapena
ndi ine womangidwa watshi: koma imva kusautswa ndi
ivangeli kwa mpamvu ya Mulungu; emwe anapulumutsa
9 ife, ndimo naitana ife ndi kuitana koyera, si kwa
ntshito zatu, koma kwa kuyerekeza kwatshi ndi kufatsa,
komwe kunapatsidwa kwa ife m' Kristu Yesu patsogolo pa
10 ntawi za magonero, koma tsopano kwasonyezedwa ndi kuone-
kera kwa Mpulumutsi watu Kristu Yesu, emwe natshotsa
imfa, natenga moyo ndi kusabvunda kwa kuunika mwa
11 ivangeli, kwa womwe dinaikidwa wouza, ndi mpostile, ndi
12 mpunzitsi. Kwa tshifukwa tshomwe dimva anso zintu
zimenezi: kosuntira sindiri ndi manyazi; kuti didziwa ie
emwe damvana, ndimo dikantshiziridwa kuti ie ali ndi
13 mpamvu ku dikira kuikirira kwanga pa siku limene. Gwira
sonyezo la mau olimba omwe wamva kwa ine, m' mvanu
14 ndi kukonda komwe kuli m' Kristu Yesu. Kuikirira
kumene kwabwino dikira mwa Nzimu Woyera womwe
ukala mwa ife.
15 Udziwa tshimene, kuti onse omwe ali m' Asiya anatembe-

nuka kwa ine; a omwe ali Figelo ndi Hermogene. Mwini 16
apatse nsisi kwa nyumba ya Onesiforo: kuti ntawi zambiri
anasangalatsa ine, ndimo sanakala ndi manyazi ndi unyolo
wanga; koma, ntawi anali m' Roma, nafuna ine ndi tshangu, 17
nandipeza (Mwini apatse kwa ie ku peza nsisi kwa Mwini 18
m' siku limene); ndimo m' zintu zambiri bwanje naimirira
pa Feso, udziwa bwino nditu.

2 Ndimo iwe, mwana wanga, limbikitsidwa m' kufatsa
komwe kuli m' Kristu Yesu. Ndimo zintu zomwe unamva 2
kwa ine mwa omariza ambiri, zomwe uikirira kwa antu
amvanu, omwe adzakala ndi mpamvu ku punzitsa ena anso.
Imva kusautswa ndi *ine*, monga wankhondo wabwino wa 3
Kristu Yesu. Palibe wankhondo pa kuimirira akodwa ie 4
eka m' zintu za moyo *umene;* kuti angosekeretsa ie emwe
nalemba ie monga wankhondo. Ndimo ngati inso muntu ayesa 5
m' masewero, wosabvekedwa tshisoti tshotshuka, kani wayesa
kwamau. Wotshita m' munda emwe atshita akanakala 6
woiamba ku gawana ndi dzobala. Ganiza ndi tshomwe 7
dinena; kuti Mwini adzapatsa iwe kudziwitsa m' zintu
zonse. Kumbukila Yesu Kristu, anauka kwa akufa, wa 8
mbeu ya Davide, kwa ivangeli wanga: momwe dimva 9
kusautswa kwa zomangira, monga wotshita zoipa; koma
mau a Mulungu osamangidwa. Ndimo dimvabe zintu 10
zonse kwa osang'kidwa, kuti awo onso angolandira kupulu-
mutsa komwe kuli m' Kristu Yesu ndi kupambana kwa
kugonera. Kumvana kuli kunena: Kuti ngati tinafa ndi 11
ie, tidzakala ndi moyo onso ndi ie: ngati timvabe, tidzawe- 12
ruza anso ndi ie: ngati tidzakana ie, ie enso adzakana ife:
ngati tiri osamvana, ie akalabe wamvanu; kuti wosadziwa 13
ku dzikana.

Ndi zintu zimenezi kumbutsa awo, kuuza *awo* m' kuona 14
kwa Mwini, kuti osatetana ndi mau, kwa kusapindula, kwa
kupondereza kwa awo omwe amva. Patsa tshangu ku 15
dzipereka wosimbidwa kwa Mulungu, wotshita emwe wosali
ndi tshifukwa ku kala ndi manyazi, kugawa bwino mau a
nteradi. Koma lambalala malongololo anko: kuti adzapiti- 16
rira m' kusapembedza, ndimo mau ao adzanyeka monga 17
kutukumira: a omwe ali Himenayo ndi Fileto; antu omwe 18
ndi nteradi anapita, kunena kuti kuukirira kunapita kali,
nagwetsa mvanu wa ena. Koma kuzika kolimbika kwa 19
Mulungu kuima, kuli ndi tshizindikilo tshimene, Mwini
adziwa awo omwe ali atshi: ndimo, Onse omwe atshula

20 dzina la Mwini atshoke kwa kusadeka. Koma m' nyumba
yeikuru dziripo si koka dziwira dza golide ndi dza silivere,
koma anso dza ntengo ndi dza dote; ndi dzina kwa ulemu,
21 ndi dzina kwa kusalemekeza. Ndimo ngati muntu adzitsuka
kwa idzo, adzakala tshiwira kwa ulemu, tshoyeretsedwa,
tshoenera kwa ntshito ya ambuiye, tshofotokozedwa kwa
22 ntshito zonse zabwino. Koma tawa mafuno aunyamata,
nutsata kudeka, mvanu, kukonda, ntendere, ndi awo omwe
23 aitana pa Mwini kwa ntima woyera. Koma mafunso opusa
24 ndi opulukira kana, kudziwa kuti abala zindeu. Ndimo
kapolo wa Mwini sakanatshita ndeu, koma akanakala waulere
25 kwa onse, wanzeru ku punzitsa, kulekereza, m' kuanja
kupunzitsa awo omwe adzikana; ngati kungokala Mulungu
angopatsa awo kutembenuza ntima kwa kudziwa kwa
26 nteradi, ndimo angodzibweza mwa khwekwe la diabolos,
kunagwidwa nkoli ndi ie kwa kufuna kwa uyu.
3 Koma dziwa tshimene, kuti m' masiku akutungo ntawi
2 zosautswa zidzafika. Kuti antu adzakala adzikonda, okonda
a ndrama, odzisamalira, onyada, onyoza, osamvera atatu
3 ao ndi amai ao, osamika, osayera, opanda kukonda kwa-
makalidwe, oumirira, onamiza, opanda kudziweruza, anka-
4 rwe, osakonda a ubwino, zinzondi, opatuka ntima, otupitswa,
5 okonda a kusekera opambana okonda a Mulungu; kugwira
makalidwe a kupembedza, koma anakana mpamvu ya iko:
6 kwa amene enso tembenuka. Kuti a amene ali awo omwe
akwawa m' zinyumba, ndimo nagwira mikoli akazi opusa
olemedwa ndi zimpulupulu, otsogozedwa ndi mafuno ena,
7 ntawi zonse kupunzira, ndimo palibe ntawi adziwa ku fika
8 kwa kudziwa kwa nteradi. Ndimo kofana monga Yane ndi
Yambre nakana Moses, tshointsho awo amene enso akana
nteradi; antu abvunditsidwa m' muwongo, otaiidwa ndi
9 mvanu. Koma sadzapitirira: kuti kupusa kwao kudza-
onedwa kwa antu onse, monga kwao onso kunafika ku
10 kala. Koma unatsata kupunzitsa kwanga, kudzitangata,
kuyerekeza, mvanu, kumva kutali, kukonda, kulongosola,
11 mazunzo, kumva; zintu zomwe zinagwa pa ine pa Anti-
yokwe, pa Koniyon, pa Listra; mazunzo anje dinamvabe:
12 ndïmo mwa awo onse Mwini napulumutsa ine. Inde, ndi
onse omwe afuna ku kala ndi moyo kopembedza m' Kristu
13 Yesu adzamva zunzo. Koma antu oipa ndi onyenga
adzakula oipa ndi oipa opambana, kunyenga ndi kunyenge-
14 dwa. Koma kala m' zintu zomwe unapunzira nulimbiki-

tsidwa nazo, kudziwa ndi omwe unapunzira izo; ndimo 15
kuti kwa kanda wadziwa malemba oyera omwe adziwa ku
panga iwe wanzeru kwa kupulumutsa mwa mvanu womwe
uli m' Kristu Yesu. Malemba onse opuziriridwa ndi 16
Mulungu *ali* inso opindulidwa kwa kupunzitsa, kwa kusu-
lumula, kwa kufotokoza, kwa kupunzitsa komwe kuli m'
kudeka: kuti muntu wa Mulungu angotetsa, kukwanitsidwa 17
kota kwa ntshito zonse zabwino.

Diuza *iwe* m' kuona kwa Mulungu, ndi kwa Kristu Yesu, 4
emwe adzaweruza amoyo ndi akufa, ndimo ndi kuonekera
kwatshi ndi dziko latshi; uza mau; kala watshangu mwa 2
nsiku, kwa nsiku; tenga kwa kuyesa, sulumula, taulira, ndi
kumva kutali konse ndi kupunzitsa. Kuti ntawi idzafika 3
ntawi sadzamvabe kupunzitsa kolimba; koma, ali ndi
makutu onyerenyetsa, adzaunjikana kwa iwo oka apunzitsi
pambuiu mafuno ao; ndimo adzatembenuza makutu ao 4
kwa nteradi, ndimo nadzalambalala kwa zintanu. Koma 5
kala wosaledzera m' zintu zonse, imva kusautswa, gwira
ntshito ya muevangeli, dzaza kuimirira kwako. Kuti kali 6
dirikutsiridwa, ndi ntawi ya kutshoka kwanga inafika.
Damenyana kumenyana kwabwino, data kupitira, dasunga 7
mvanu: kwa ntawi imene tshiikidwa kwa ine tshisoti tsho- 8
tshuka tsha kudeka, tshomwe Mwini, Woweruza wodeka,
adzapatsa kwa ine pa siku limene: ndimo si koka kwa ine,
koma anso kwa awo onse omwe mwakonda kuonekera
kwatshi.

Tshita tshangu tshako ku fika kwa ine nsanga: kuti 9, 10
Dema naleka ine, anakonda kugonera kumene kwatsopano,
natshoka kwa Tesalonika; Kreske ku Galatiya, Tito kwa
Dalmatiya. Luka eka ali ndi ine. Tenga Marko, ndimo 11
tenga ie ndi iwe: kuti ali wotshita kwa ine kwa kuimirira.
Koma Tikiko dinatumiza ku Feso. Tshopfundira tshomwe 12, 13
dinasia pa Trowa ndi Karpo, tenga ntawi ufika, ndi mabuku,
kopambana dzikopa. Alesandire wosula-nsambo natshita 14
ine tshoipa tshambiri: Mwini adzabweza kwa ie kwa
ntshito zatshi: wa emwe utshenjera anso; kuti anakana 15
kwambiri mau atu. Pa kudzikana kwanga koiamba palibe 16
modzi nakala pa pande langa, koma onse naleka ine:
kusawereng'jedwe kwa awo. Koma Mwini naima ndi ine, 17
nalimbitsa ine; kuti mwa ine mau anangouzidwa kota, ndi
kuti Mitundu yonse inangomva: ndimo dinapulumutsidwa
kwa nkamwa mwa nkango. Mwini adzapulumutsa ine kwa 18

ntshito zonse zoipa, ndimo adzapulumutsa ine kwa dziko
latshi lamwamba: kwa emwe *kukale* kupambana kwa
magonero a magonero. Amen.
19 Utsa Priska ndi Akwila, ndi nyumba ya Onesiforo.
20 Erasto nakala pa Korinte: koma Trofimo dinasia pa Mileto
21 wodwala. Tshita tshangu tshako ku fika patsogolo pa
malimwe. Yubulo autsa iwe, ndi Pude, ndi Lino, ndi
Kladiya, ndi abali onse.
22 Mwini akale ndi nzimu wako. Kufatsa kukale ndi iwe.

---

## EPISTOLA LA PAULOS KWA

# TITO.

1 PAULOS, kapolo wa Mulungu, ndi mpostile wa Yesu
Kristu, kwa mvanu wa osang'kidwa a Mulungu, ndi ku-
2 dziwa kwa nteradi komwe kuli kwa kupembedza, m' kulinga-
lira kwa moyo wosamariza, womwe Mulungu, emwe wosadziwa
3 ku nama, nalonjezana patsogolo ntawi zosamariza; koma m'
nsiku zatshi nasonyeza mau atshi m' kuuza, ndi komwe
4 dinamvanidwa kwa mau a Mulungu Mpulumutsi watu; kwa
Tito, mwana wanga woona pambuiu mvanu wa tonse:
Kufatsa ndi ntendere kwa Mulungu Atate ndi Kristu Yesu
Mpulumutsi watu.
5 Kwa tshifukwa tshimene dinasia iwe m' Krete, kuti
ukandandalitsa zintu zomwe zinasowedwa, nukaika akuru m'
6 mizinda yonse, monga dinauza iwe; ngati muntu modzi ali
wopanda tshulo, mamuna wa nkazi modzi, ali ndi ana omwe
amvana, omwe osatshulidwa ndi kusaluka kapena atshiwawa.
7 Kuti woyang'anira akanakala wopanda tshulo, monga ndindo
wa Mulungu; si wodzisamalira, si wokwia nsanga, si
wolongolola, si womenya, si woumira wa ndrama zonyansa;
8 koma wosungira alendo, wokonda wa ubwino, wodziweruza,
9 wodeka, woyera, wosaledzera; kugwira mau a mvanu omwe
ali kwa kupunzitsa, kuti angodziwa ku taulira m' kupu-
nzitsa kolimba, ndi ku tshimika akana.
10 Kuti alipo antu ambiri atshiswawa, alankula autsiru

ndi onyenga, kopambana awo a kudula, nkamwa mwa omwe 11
mukanatsekedwa; antu omwe atembenuza nyumba zonse,
kupunzitsa zintu zomwe sakana*punzitsa*, kwa ndrama
zonyansa. Modzi wa awa oka, mprofeti wa awo, nati, Akrete 12
ntawi zonse ali onama, dzirombo dzoipa, osusuka olesi.
Kumariza kumene kuli kwanteradi. Kwa tshifukwa 13
tshimene sulumula awo kolimba, kuti angokala olimba mu
mvanu, si kusamala ntanu za Ayuda, ndi mau a antu omwe 14
atembenuka kwa nteradi. Kwa oyera zintu zonse ziri 15
zoyera: koma ku awo omwe ali odetsedwa ndi osamvana
palibe kantu kali koyera; koma muwongo wao ndi ku-
dzidziwitsa kwao zidetsedwa. Abvomera kuti adziwa 16
Mulungu ; koma ndi ntshito zao akana ie, ali onyansa, ndi
osamvera, ndi kwa ntshito zonse zabwino otaiidwa.

Koma lankula zintu zomwe zikala bwino ndi kupunzitsa 2
kolimba: kuti antu ogonera akale osaledzera, ape, odziweruza, 2
olimba mwa mvanu, m' kukonda, m' kulongosola: kuti akazi 3
ogonera anso akale odzinga m' makalidwe, si anseke kapena
osagwidwa ndi vinyo wambiri, apunzitsi a tshimene tshomwe
tshiri tshabwino; kuti angopunzitsa akazi ang'ono ku konda 4
amuna ao, ku konda ana ao, *ku kala* odziweruza, oyera, 5
otshita pa kwao, okoma, kukala pansi pa amuna ao, kuti
mau a Mulungu osatukwanidwa: amuna ang'ono onso 6
taulira ku kala odziweruza: m' zintu zonse kudzisonya sonyo 7
la ntshito zabwino; m' kupunzitsa kwako *kusonya* kusa-
bvunda, upe, kunena kolimba, komwe kusadziwidwa ku 8
sutsidwa; kuti ie emwe ali wa pande lapandunji angopa-
tsidwa manyazi, wosali ndi kantu koipa ku nena ndi ife.
*Taulira* akapolo ku kala pansi pa ambuiye ao, *ndimo* ku 9
kala osekeretsa *ku awo* m' zintu zonse ; si kukana ; si kuba, 10
koma kusonya mvanu wabwino wonse; kuti angokometsa
kupunzitsa kwa Mulungu Mpulumutsi watu m' zintu zonse.
Kuti kufatsa kwa Mulungu kwaonekera, kutenga kupulu- 11
mutsa kwa antu onse, kupunzitsa ife, kwa kuyerekeza kuti, 12
kukana kusapembedza ndi mafuno adziko, tikakala ndi
moyo kosaledzera ndi kodeka ndi kopembedza m' kugonera
kwatsopano kumene; kuyang'ana kwa kulingalira kodala 13
ndi kuonekera kwa kupambana kwa Mulungu watu wang'-
kuru ndi Mpulumutsi Yesu Kristu; emwe anadzipatsa kwa 14
ife, kuti anangoombola ife kwa mpulupulu zonse, nango-
yeretsa kwa ie eka antu kwa kupotshera kwatshi, atshitsanzo
a ntshito zabwino.

15 Zintu zimenezi lankula ndi taulira ndi sulumula ndi mau
onse. Palibe muntu anyoze iwe.

3 Kumbutsa awo ku kala pansi pa oweruza, pa ampamvu,
ku kala omvera, ku kala ota kwa ntshito yonse yabwino,
2 ku nena koipa ndi palibe muntu, si ku kala andeu, ku kala
3 aulere, kusonya kuanja konse kwa antu onse. Kuti ife
enso ntawi yapita tinali opusa, osamvera, onyengedwa,
kuimirira mafuno ena ndi masekero, kukala ndi moyo m'
4 kwaipa ndi m' dano, okwiidwa, kukwiirana. Koma ntawi
kukoma kwa Mulungu Mpulumutsi watu, ndi kukonda
5 kwatshi kwa antu, kunaonekera, si ndi ntshito *zotshitidwa*
m' kudeka, zomwe tinatshita ife toka, koma kwa nsisi yatshi
natipulumutsa, mwa kutsuka kwa kubadwa anso ndi ku-
6 fotokoza kwa Nzimu Woyera, womwe natsanula pa ife
7 kolemera, mwa Yesu Kristu Mpulumutsi watu; kuti, ku-
deketsedwa ndi kufatsa kwatshi, tinangopangidwa oloa
8 kwa kulingalira kwa moyo wosamariza. Kunena kuli
komvana, ndimo ndi zintu zimenezi difuna kuti utshimika
ndi nteradi, kwa nsonga kuti awo omwe anamvana ndi
Mulungu angosamala ku gwira ntshito zabwino. Zintu
9 zimenezi ziri zabwino ndi zopindulidwa kwa antu: koma
lambalala mafunso opusa, ndi mafuko, ndi zindeu, ndi
mamenyano ndi mau; kuti ziri zosapindula ndi zautsiru.
10 Muntu emwe ali wanjiru pambuiu kuambirira kwatshimodzi
11 ndi kwatshiwiri kaniza; kudziwa kuti modzi wotere atembe-
nuzidwa, natshimwa, kudzisutsidwa.

12 Ntawi didzatumiza Artema kwa iwe, kapena Tikiko, kala
ndi tshangu ku fika kwa ine ku Nikopolis: kuti uko
13 dayerekeza ku kala malimwe. Perekeza Zena nkoswe ndi
Apolo pa ulendo pao kwatshangu, kuti palibe kantu
14 kasowedwe ku awo. Ndimo *antu* atu unso apunzire ku gwira
zintu zabwino kwa zotshitira zofunidwa, kuti osakala opanda
dzobala.

15 Onse omwe ali ndi ine autsa iwe. Utsa awo omwe akonda
ife mwa mvanu.

Kufatsa kukale ndi inu nonse.

## EPISTOLA LA PAULOS KWA

# FILEMON.

PAULOS, womangidwa wa Kristu Yesu, ndi Timote 1
mbali watu, kwa Filemon wokondedwa watu ndi
wotshita nzatu, ndi kwa Apiya mlongo watu, ndi kwa 2
Arkipo wankhondo nzatu, ndi kwa eklesia m' nyumba yako:
Kufatsa kwa inu ndi ntendere kwa Mulungu Atatu atu ndi 3
Mwini Yesu Kristu.

Dinena tshakoma kwa Mulungu wanga ntawi zonse, 4
kutshula ndi iwe m' mapempero anga, kumva ndi kukonda 5
kwako, ndimo ndi mvanu womwe upotshera kwa Mwini
Yesu, ndi kwa oyera onse; kuti unzatshi wa mvanu wako 6
ungokala wotetsa, m' kudziwa kwa zintu zonse zabwino
zomwe ziri mwa inu, kwa Kristu. Kuti dinali ndi 7
tshimwemwe tshambiri ndi kusangalatsa m' kukonda kwako,
tshifuka mitima ya oyera inasangalatsidwa mwa iwe, mbali.

Mwa kuti, ngati dipotshera kulimbika konse m' Kristu ku 8
uza iwe tshimene tshomwe tshiri tshabwino, kosuntira kwa 9
kukonda kopambana dipempa, diri modzi wotere monga
Paulos mkuru, ndimo tsopano womangidwa anso wa Kristu
Yesu: dipempa iwe kwa mwana wanga, emwe dabala m' 10
zomangira zanga, Onesimo, emwe ntawi yapita anali 11
wosapindulidwa kwa iwe, koma tsopano ali wopindulidwa
kwa iwe ndi kwa ine: emwe dinabweza ie eka kwa iwe, 12
kumene kuli, ntima wanga nditu: emwe dinafuna ku sunga ndi 13
ine, kuti kwa iwe anangoimirira kwa ine m' zomangira za iva-
ngeli: koma wopanda muwongo wako sindifuna ku tshita kantu; 14
kuti ubwino wako sukanakala monga ndi uko, koma kwa
kufuna kwaufulu. Kuti kapena ndimo anatshotsedwa *kwa iwe* 15
kwa nsiku, kuti ukapotshera ie kwa ntawi zonse; si ntawi ina 16
monga kapolo, koma wopambana kapolo, mbali wokondedwa,
kopambana kwa ine, koma bwanje kopambana kwa iwe, m'
nyama ndi m' Mwini. Ngati pomwe uwerenga ine woga- 17
wana, landira ie monga ine ndeka. Koma ngati watshi- 18
mwitsa iwe m' kantu, kapena akong'gola *iwe* kantu, ika
kamene pa ine; ine Paulos dikalemba ndi dzanja langa loka, 19

didzakabweza: kuti sindinena kwa iwe bwanje kuti ukong'-
20 gola kwa ine inde iwe eka kopambana. Inde, mbali, leka
ine ku potshera tshimwemwe kwa iwe m' Mwini: sangalatsa
21 ntima wanga m' Kristu. Kupotshera mvanu m' kumvera
kwako dilemba kwa iwe, kudziwa kuti udzatshita inde
22 kopambana komwe dinena. Koma ndi inso fotokozera ine
enso pokala: kuti dilingalira kuti mwa mapempero anu
didzapatsidwa kwa inu.
23 Epafra, womangidwa nzanga m' Kristu Yesu, autsa iwe;
24 *ndimo tshointsho atshita* Marko, Aristarko, Dema, Luka,
otshita-anzanga.
25 Kufatsa kwa Mwini watu Yesu Kristu kukale ndi nzimu
wako. Amen.

---

EPISTOLA KWA

# A H E B E R E.

1 MULUNGU, kali analankula kwa atate m' aprofeti ndi
2 mapande ena ndi m' makalidwe ena, pa nsonga ya
masiku amene analankula kwa ife m' Mwana *watshi*, emwe
naika woloa m' zintu zonse, mwa emwe enso napanga
3 magonero; emwe ali kuwala kwa kupambana kwatshi, ndi
fanizo nditu la ntsemerero watshi, ndi kukulitsa zintu zonse
ndi mau a mpamvu yatshi, ntawi anapanga kusambitsa kwa
zakwaipa, nakala pansi pa dzanja lamanja la Ukulu pa
4 mwamba; anakala ndi tshointsho wabwino wopambana
anjelo, monga waloa m' dzina labwino kwambiri lopambana
5 awo. Kuti kwa ani a anjelo nati pa ntawi imodzi,

Uli Mwana wanga,
Siku limene dabala iwe?

ndi inso,

Didzakala kwa ie Atate,
Ndimo adzakala kwa ine Mwana?

6 Ndimo ntawi inso aloeza wobadwa woiamba m' dziko
7 anena, Ndimo anjelo onse a Mulungu apembedze ie. Ndimo
ndi anjelo ati,

Emwe apanga anjelo atshi zimpepo,
Ndi oimirira atshi lilume la moto:
koma ndi Mwana *ati*, 8
Mpando wotshuka wako, O Mulungu, uli kwa kugonera wa kugonera;
Ndi ndodo yatshifumu ya kudeka iri ndodo yatshifumu ya dziko lako.
Wakonda kudeka, ndimo wakwiira mpulupulu; 9
Ndimo Mulungu, Mulungu wako, wadzosa iwe
Ndi mafuta a kukondwera pamwamba anzako.
Ndimo, 10
Iwe, Mwini, m' kuamba waika kuzika kwa dziko,
Ndi miamba iri ntshito za manja ako:
Idzamwaza; koma ukalabe: 11
Ndimo iyo yonse idzakala yakali monga mwinjiro;
Ndimo monga tshopfunda udzaipinda, 12
Monga mwinjiro, ndimo idzasintanidwa:
Koma uli modzimodzi,
Ndimo dzaka dzako sidzidzata.
Koma ndi ani a anjelo wanena pa ntawi imodzi, 13
Kala pa dzanja lamanja langa,
Kwa ntawi dipanga maliwongo ako mpando wa mapazi ako?
Kodi osali onse mizimu yoimirira, otumidwa ku imirira 14
kwa awo omwe adzaloa m' kupulumutsa?

Ndimo tikanasamala kolimba kopambana kwa zintu 2
zomwe zinamvedwa, kani kapena tikweng'kwenuka *kwa izo.*
Kuti ngati mau analankulidwa mwa anjelo nakala kolimbi- 2
tsidwa, ndi matshimo onse ndi kusamvera zinalandira kuli-
pira kodeka kwa kusekeretsa; bwanje tidzapulumuka, 3
ngati tisasamala kupulumutsa kwakukuru kotere? komwe
pa kwiamba kunalankulidwa mwa Mwini, kunatshimikidwa
kwa ife ndi awo omwe anamva; Mulungu unso kumariza 4
ndi awo, ndimo ndi zizindikilo ndi zozizwa, ndimo ndi
mpamvu zambiri, ndimo ndi mitulo ya Nzimu Woyera, kwa
kufuna kwatshi.

Kuti si kwa anjelo anaika pansi dziko lirinkudza, ndi 5
lomwe tilankula. Koma modzi m' malo ena wamariza, 6
kuti,
Muntu ali ani, kuti ukumbukila ie?
Kapena mwana wa muntu, kuti utsheza nai'?
Wapanga ie pansi wang'ono wopambana anjelo; 7

Wabveka ie ndi tshisoti tshotshuka, ndi kupambana ndi ulemu,
Ndimo waika ie pamwamba pa ntshito za manja ako:
8 Waika zintu zonse pansi pa mapazi atshi.
Kuti m' tshimene naika zintu zonse pansi pa ie, nasia
tshabe tshomwe tshosaikidwa pansi pa ie. Koma tsopano
9 kosuntira sitiona zintu zonse zaikidwa pansi pa ie. Koma
tiona ie emwe wapangidwa pansi wang'ono wopambana
anjelo, *inde* Yesu, tshifuka tsha kumva kwa imfa wabveke-
dwa tshisoti tshotshuka ndi kupambana ndi ulemu, kuti ndi
10 kufatsa kwa Mulungu akalawa imfa kwa *antu* onse. Kuti
kunakalitsa ie, kwa emwe ziri zintu zonse, ndi mwa emwe
ziri zintu zonse, m' kutenga ana ambiri kwa kupambana, ku
panga woiamba wa kupulumutsa kwao wakuta mwa kumva.
11 Kuti ie emwe ayeretsa ndi awo omwe ayeretsedwa ali onse a
modzi: kwa tshifukwa tshimene wosali ndi manyazi ku
12 tsha awo abali, kunena,
Didzauza dzina lako kwa abali anga,
M' kati mwa eklesia didzaimba kul'emekeza kwako.
13 Ndimo onso, Didzaika kumvana kwanga mwa ie. Ndimo
14 onso, Ona, ine ndi ana omwe Mulungu wandipatsa. Ndimo
monga ana ali ogawana m' nyama ndi m' mwazi, ie eka anso
modzimodzi nagawana m' zimene; kuti mwa imfa angotenga
kwa tshabe ie emwe apotshera mpamvu ya imfa, emwe ali,
15 diabolos; ndimo angopulumutsa onse awo omwe mwa kuopa
kwa imfa anali ntawi ya moyo wao wonse pansi pa umpawi.
16 Kuti nditu wosagwira anjelo, koma agwira mbeu ya
17 Abraham. Ndimo kunali kufunidwa kwa ie m' zintu zonse
ku pangidwa wofana ndi abali atshi, kuti anangokala
ndzukuru wang'kuru wansisi ndi wamvanu m' zintu za
18 Mulungu, ku pereka dipo kwa mpulupulu za antu. Kuti
m' tshimene ie eka wamva kuyesedwa, ali ndi mpamvu ku
tangatira omwe ayesedwa.

3 Mwa kuti, abali oyera, ogawana ndi kuitana kwaku-
mwamba, ganiza ndi Mpostile ndi Ndzukuru wang'kuru wa
2 kubvomereza kwatu, *inde* Yesu; emwe anali wamvanu
kwa ie emwe anaika ie monga anso Moses anali m' nyumba
3 yatshi yonse. Kuti wawerengedwa woenera wa kupambana
wopambana Moses, ndi kutshuruka monga ie emwe namanga
4 nyumba wapotshera ulemu wopambana nyumba. Kuti
nyumba zonse zimangidwa ndi modzi; koma ie emwe
5 namanga zintu zonse ali Mulungu. Ndimo Moses nditu

anali ndi mvanu m' nyumba yatshi yonse monga wosunga,
kwa kumariza kwa zintu zidya zomwe zinali ku lankulidwa
pambuiu; koma Kristu monga mwana, pa nyumba yatshi; 6
nyumba ya emwe tiri, ngati tigwira bwino kulimbika kwatu
ndi kupambana kwa kulingalira kwatu kolimba kwa nsonga.
Ndimo, inde monga Nzimu Woyera unena, 7

Lero ngati mudzamva liu latshi,
Musalimbitsa mitima yanu, monga m' kubvuta, 8
Kofana monga m' siku la kuyesa m' tshipululu,
Ndi komwe atatu anu nayesa *ine* ndi kuyang'anira *ine*, 9
Ndimo naona ntshito zanga dzaka makumi anai.
Mwa kuti dinakwiitsidwa ndi fuko limene, 10
Ndinati, Ntawi yonse atshimwa m' mitima yao:
Koma sanadziwa njira zanga;
Monga dinalumbira m' kukwiira kwanga, 11
Sadzaloa mwa kupuma kwanga.

Yang'anirani, abali, kani kapena kudzali m' wina wa inu 12
ntima woipa wa kusamvana, m' kuleka kwa Mulungu wa-
moyo: koma tauliranani siku ndi siku, monga ntawi 13
monga tshitshedwa Lero; kani modzi wa inu wolimbi-
tsidwa ndi tshinyengo tsha mpulupulu: kuti tinakala 14
ogawana ndi Kristu, ngati tigwira bwino kuamba kwa ku-
mvana kwatu kolimba kwa nsonga: ntawi tshinenedwa, 15

Lero ngati mudzamva liu latshi,
Musalimbitsa mitima yanu, monga m' kubvuta.

Kuti ani, ntawi anamva, anabvuta? iai, kodi si awo onse 16
omwe anaturuka mwa Yiputa ndi Moses? Ndimo ndi ani 17
anakwiitsidwa dzaka makumi anai? kodi si kunali ndi awo
omwe anatshimwa, mitembo ya omwe inagwa m' tshipululu?
Ndimo kwa ani analumbira kuti sakaloa m' kupuma 18
kwatshi, koma kwa awo omwe anali osamvera? Ndimo 19
tiona kuti sanadziwa ku loa tshifuka tsha kusamvana.

Ndimo tiope, kani kapena, lonjezano linasiidwa la kuloa 4
mwa kupuma kwatshi, modzi wa inu akaenedwa kunapere-
weza. Kuti nditu tapotshera makalidwe abwino anauzidwa 2
kwa ife, inde monga anso awo: koma mau a kumva osana-
pindulitsa awo, tshifuka sanakomaniza ndi mvanu ndi awo
omwe anamva. Kuti ife tomwe tamvana tiloa m' kupuma 3
kumene; inde monga wanena,

Monga dinalumbira m' kukwiira kwanga,
Sadzaloa m' kupuma kwanga:

monga ngati ntshito zinata kwa kuzika kwa dziko. Kuti 4

wanena m' malo ena ndi *siku* latshisanu ndi tshiwiri
tshointsho, Ndimo Mulungu napuma pa siku latshisanu ndi
5 tshiwiri kwa ntshito zatshi zonse; ndimo m' *malo* amene enso,
Sadzaloa m' kupuma kwanga.
6 Ndimo kuona kuti kutsala kuti ena akaloa momwe, ndimo
awo kwa omwe makalidwe abwino anauzidwa kali napere-
7 weza ku loa tshifuka tsha kusamvera, anso atshula siku
limodzi, kunena m' Davide, pambuiu pa ntawi yeitali
tshointsho, Lero, monga wanenedwa kali,
Lero ngati mudzamva liu latshi,
Musalimbitsa mitima yanu.
8 Kuti ngati Yoshuwa anapatsa awa kupuma, sakanalankula
9 pambuiu ndi siku lina. Ndimo kutsala kupuma kwa-
10 sabata kwa antu a Mulungu. Kuti ie emwe analoa m'
kupuma kwatshi ie eka anso anapuma kwa ntshito zatshi,
11 monga Mulungu natshita kwa zatshi. Ndimo tipatse
tshangu ku loa m' kupuma kumene, kuti palibe muntu agwe
12 pambuiu sonyezo lomwe la kusamvera. Kuti mau a
Mulungu ali amoyo, ndi atshangu, ndi akutwa opambana
mpeni wina wankondo wakutwa konse, ndimo kubola inde
kwa kugawa ndi moyo ndi nzimu, ndimo ndi zimfundo ndi
nsiwe, ndimo ansangu ku dziwitsa maganizo ndi matintu za
13 ntima. Ndimo palibe wopangidwa emwe wosali wosonyedwa
m' kuona kwatshi: koma zintu zonse ziri zamariseke ndi
zinaikidwa poyera patsogolo pa maso pa ie ndi emwe tiri ndi
ku tshita.
14 Ndimo kupotshera ndzukuru wang'kuru wopambana, emwe
wapita mwa miamba, Yesu Mwana wa Mulungu, tigwire
15 kolimba kubvomereza kwatu. Kuti sitipotshera ndzukuru
wang'kuru emwe wosadziwa ku tosedwa ndi kumva kwa
mafoko atu; koma modzi emwe wayesedwa m' zintu zonse
16 kofana *tiri*, *koma* wopanda mpulupulu. Ndimo tiyandike
ndi kulimbika kwa mpando wotshuka wa kufatsa, kuti
tingolandira nsisi, ntingopeza kufatsa ku tangata *ife* m'
ntawi ya kufunidwa.

5 Kuti adzukuru akuru onse, anatengedwa kwa mwa antu,
aikidwa kwa antu m' zintu za Mulungu, kuti angotsira
2 ndi mitulo ndi zinsembe kwa zimpulupulu: emwe adziwa
ku mva kwaulere ndi akupulukira ndi atshimo, tshifuka kuti
3 ie eka anso azungulidwa ndi kufoka, ndimo ndi tshifukwa
tsha kumene, monga kwa antu, tshointsho onso kwa ie eka,
4 akanatsira kwa zimpulupulu. Ndimo palibe muntu atenga

ulemu kwa ie eka, koma ntawi aitanidwa ndi Mulungu, inde
monga anali Haron. Tshointsho Kristu unso sanadzipa- 5
mbanitsa ku pangidwa ndzukuru wang'kuru, koma ie emwe
nalankula kwa ie,

> Uli Mwana wanga,
> Siku limene dabala iwe:

monga anena anso m' *malo* ena, 6

> Uli ndzukuru kwa magonero
> Pambuiu makalidwe a Melkizedeki.

Emwe m' masiku a nyama yatshi, kunatsira mapempero ndi 7
mapempo ndi kulira kolimba ndi misozi kwa ie emwe
anali ndi mpamvu ku pulumutsa ie kwa imfa, ndimo
kunamvedwa kwa kuopa kopembedza kwatshi, ngati anali 8
Mwana, kosuntira napunzira kumvera ndi zintu zomwe
anamva; ndimo kunatetsedwa, nakala kwa awo onse omwe 9
amvera ie tshifukwa tsha kupulumutsa kosamariza;
atshedwa ndi Mulungu ndzukuru wang'kuru pambuiu 10
pa makalidwe a Melkizedeki.

Wa emwe tiri ndi zintu zambiri ku nena, ndi zolimba 11
za kusanduka, kuona mukala ogonta pang'ono. Kuti ntawi 12
ndi tshifukwa tsha ntawi mukanakala apunzitsi, mwafuna
anso kuti wina apunzitsa inu oiamba a oiamba a mau a
Mulungu; ndi mukala otere monga muli ndi kufunidwa ndi
nkaka, ndimo si kwa kudia kolimba. Kuti ie emwe 13
agawa ndi kaka ali wopanda kudziwa kwa mau a kudeka;
kuti ali kanda. Koma kudia kolimba kuli kwa antu a 14
nsing'ku woukuru, *inde* adya omwe ndi tshifukwa ndi
kutshita apotshera madziwiko ao odzitshitidwa ku dziwitsa
ubwino ndi kwaipa.

Mwa kuti kuleka mau a kuamba kwa Kristu, tifulumire 6
kwa kuta; si kuika anso kuzika kwa kutembenuza ntima
kwa ntshito zakufa, ndi kwa mvanu kwa Mulungu, kwa 2
kupunzitsa kwa mabapatisma, ndi kwa kuika kwa manja,
ndi kwa kuukirira kwa akufa, ndi kwa kuweruza kosama-
riza. Ndimo tshimene tidzatshita, ngati Mulungu alola. 3
Kuti monga ndi awo omwe ntawi imodzi anaunikidwa na- 4
lawa ndi ntulo wakumwamba, napangidwa ogawana a Nzimu
Woyera, ndimo nalawa ndi mau abwino a Mulungu, ndi 5
mpamvu za kugonera kulinkudza, ndimo *pomwe* anagwa, 6
kuli kusadziwa ku ta ku fotokoza awo onso kwa kutembe-
nuza ntima; kuona apatshika ku awo oka Mwana wa
Mulungu unso, naika ie pa manyazi poyera. Kuti dziko 7

lomwe lamwa mvula yomwe ifika ntawi zambiri pa ilo,
ndimo libala zitsamba zaubwino kwa awo kwa omwe enso
8 lilimidwa, lilandira kudala kwa Mulungu: koma ngati
libala minga ndi mitungwi, litaiidwa ndimo liri pafupi ndi
tukwano; nsonga ya lomwe iri ku otshedwa.
9 Koma, okondedwa, tikantshiziridwa zintu zabwino zopa-
mbana ndi inu, ndi zintu zomwe zipatikana kupulumutsa,
10 ngati tilankula tshointsho: kuti Mulungu wosali wosadeka
ku iwala ntshito yanu ndi kukonda komwe munasonya kwa
dzina latshi, m' tshomwe munaimirira kwa oyera, ndimo
11 muimirira tsopano. Ndimo tifuna kuti onse a inu angosonya
tshangu tshimene kwa kudzaza kwa kulingalira inde kwa
12 nsonga: kuti simungokala otshedwa, koma ofanizira a awo
omwe mwa mvanu ndi kulongosola aloa malonjezano.
13 Kuti ntawi Mulungu nalonjezana kwa Abraham, tshifuka
sanadziwa ku lumbira ndi palibe modzi wang'kuru wopa-
14 mbana, nalumbira ndi ie eka, kuti, Nditu kudala didzadalitsa
15 iwe, ndi kupindula didzapindula iwe. Ndimo tshointsho,
16 kunamvabe kolongosola, nalandira lonjezano. Kuti antu
alumbira ndi wang'kuru wopambana: ndimo m' makanga-
17 no onse ao lumbiro liri kuta kwa kulimbitsa. Mwa lomwe
Mulungu, kufuna ku sonyeza kutshuruka kopambana kwa
oloa a lonjezano kusasintanitsa kwa kuweruza kwatshi,
18 nalekanitsa ndi lumbiro: kuti ndi zintu ziwiri zosasintanitsa,
m' zomwe kuli kusadziwa ku ta kwa Mulungu ku nama,
tingopotshera kufulumiza kolimba, omwe tinatawa kwa
kupulumuka ku gwira kulingalira kuikidwa patsogolo pa
19 ife; komwe tipotshera monga nangula wa nzimu, *kuli-*
*ngalira* koikidwa ndi kolimba ndimo kuloa m' tshimene
20 tshomwe tshiri m' bwalo mwa tshopimba; pomwe monga
wotamanga patsogolo Yesu naloa kwa ife, kunakala ndzu-
kuru wang'kuru kwa ntawi yonse pambuiu makalidwe a
Melkizedeki.
7 Kuti Melkizedeki amene, fumu yotshuka ya Salem,
ndzukuru wa Mulungu Wang'kuru Wopambana, emwe
nakomana ndi Abraham kubwera kwa kupa kwa mafumu
2 otshuka, nadalitsa ie, kwa emwe enso Abraham anagawa
pande lakumi kwa zonse (ali woiamba, ndi kusanduka,
Fumu Yotshuka ya kudeka, ndimo pomwe enso Fumu
Yotshuka ya Salem, omwe ali, Fumu Yotshuka ya ntendere;
3 wopanda atate, wopanda amai, wopanda fuko, kupotshera
kapena palibe kuiamba kwa masiku kapena palibe nsonga

ya moyo, koma wapangidwa wofana ndi Mwana wa
Mulungu), akalabe ndzukuru.
Koma ganizani wang'kuru bwanje muntu amene anali, kwa 4
emwe Abraham, mbuiye wang'kuru, napatsa pande lakumi
mwa zankondo zopambana. Ndimo awa nditu a ana a 5
Levi omwe alandira udzukuru apotshera mau ku tenga
mapande a makumi kwa antu ndi mau, omwe ali, a abali
ao, ngati awo anaturuka mwa dziuno dza Abraham: koma 6
ie, fuko la emwe losawerengedwa kwa awo, watenga
mapande a makumi kwa Abraham, ndimo wadalitsa ie emwe
apotshera malonjezano. Koma kopanda kukangana kwina 7
wang'ono wodalitsidwa ndi wopambana. Ndimo pano antu 8
omwe afa alandira mapande a makumi; koma apo modzi,
ndi emwe kumarizidwa kuti akala ndi moyo. Ndimo, ku 9
nena tshointsho, mwa Abraham inde Levi, emwe alandira
mapande a makumi, walipira mapande a makumi; kuti 10
anali kosuntira m' dziuno dza atatu atshi, ntawi Melkizedeki
nakomana nai'.
Ndimo ngati kunali kuta mwa udzukuru Walevi (kuti 11
pansi pa iwo antu analandira mau), kufunidwa kwina *kunali*
kwanje kuti ndzukuru wina akauka pambuiu pa makalidwe
a Melkizedeki, ndimo wosawerengedwa pambuiu pa maka-
lidwe a Haron? Kuti udzukuru unasintanidwa, kupangidwa 12
kwa kufunidwa kusinta anso kwa mau. Kuti ie wa emwe 13
zintu zimenezi zinenedwa agawana ndi fuko lina, kwa lomwe
palibe muntu wapatsa kuimirira pa katshisi. Kuti kuene- 14
kera kuti Mwini watu wauka kwa Yuda; monga ndi fuko
lomwe Moses sanalankula kantu ndi adzukuru. Ndimo tsho- 15
mwe *tinena* tshiri kosuntira tshoenekera kopambana, ngati
pambuiu kufana kwa Melkizedeki auka ndzukuru wina,
emwe wapangidwa, si pambuiu pa mau a kuuza kwanyama, 16
koma pambuiu pa mpamvu ya moyo wosamariza: kuti 17
kumarizidwa *ndi ie*,

Uli ndzukuru kwa magonero
Pambuiu pa makalidwe a Melkizedeki.

Kuti kuli kutshotsa kwa mau atsogolo tshifuka tsha kufoka 18
kwatshi ndi kusapindulidwa (kuti mau sanapanga kantu 19
kota), ndi kuloeza pa omwe kulingalira kwabwino kopa-
mbana, mwa komwe tiyandika kwa Mulungu. Ndimo m' 20
monga ambiri monga si *kuli* kopanda ku tenga lumbiro
(kuti awo nditu anapangidwa adzukuru opanda lumbiro; 21
koma ie ndi lumbiro ndi ie emwe anena ndi ie,

Mwini nalumbira ndimo wosadzadzitembenuka
Uli ndzukuru kwa magonero);
22 ndi tshointshi ambiri inso Yesu wakala wotangatira wa
23 kupangana kwabwino kopambana. Ndimo awo nditu
anapangidwa adzukuru ambiri m' kutshuruka, tshifuka
24 kuti ndi imfa aletsedwa kwa kukalabe: koma ie, tshifuka
akala kwa ntawi yonse, apotshera udzukuru watshi wosasinta.
25 Mwa kuti inso ali ndi mpamvu ku pulumutsa kota awo
omwe ayandika kwa Mulungu mwa ie, kuona akala ndi
moyo ntawi yonse ku letsetsa kwa awo.
26 Kuti ndzukuru wang'kuru wotere nakalitsa ife, woyera,
wopanda tshinyengo, wosadetsedwa, wogawidwa kwa
ampulupulu, ndimo watalikitsidwa kopambana miamba;
27 emwe wosafuna masiku onse, wofana ndi adzukuru akuru
adya, ku tsira zinsembe, poiamba kwa zakwaipa zatshi, ndi
pomwe kwa *zakwaipa* za antu: kuti kumene natshita kamodzi
28 kwa onse, ntawi natsira ie eka. Kuti mau aika antu
adzukuru akuru, ali ndi kufoka; koma mau a lumbiro,
omwe anali pambuiu pa mau, *aika* Mwana, wotetsedwa kwa
ntawi yonse.
8 Ndimo m' zintu zomwe tirikunena nsonga yopambana *iri
imene:* Tiri ndi ndzukuru wang'kuru wotere, emwe nakala
pansi pa dzanja lamanja la mpando wotshuka wa Ukuru m'
2 miamba, woimirira wa zintu zoyera, ndi wa msasa woona,
3 womwe Mwini anamanga, si muntu. Kuti adzukuru akuru
onse aikidwa ku tsira mitulo ndi zinsembe: mwa kuti kuli
kufunidwa kuti *ndzukuru wang'kuru* amene enso apotshera
4 kantu ku tsira. Ndimo ngati anali pa dziko, sakakala
ndzukuru konse, kuona alipo adya omwe atsira mitulo kwa
5 mau; omwe aimirira *tshimene tshomwe tshiri* tshofaniza ndi
ntunzi za zintu zamwamba, inde monga Moses aambiriridwa
*ndi Mulungu* ntawi anatofuna ku manga msasa: kuti, Ona,
ati, kuti upanga zintu zonse kwa sonyezo lomwe linaso-
6 nyedwa kwa iwe m' piri. Koma tsopano walandira kuimirira
kwabwino kopambana, ndi bwanje ambiri inso ali woleka-
nitsa wa kupangana kwabwino kopambana, komwe kwa-
7 tshitidwa pa malonjezano abwino opambana. Kuti ngati
*kupangana* kumene koiamba kunakala kopanda tshimo,
8 pomwe palibe malo akafunidwa kwa kwatshiwiri. Kuti
kupeza tshimo ndi awo, ati,
Ona, masiku afika, ati Mwini,
Kuti didzapanga kupangana kwatsopano ndi nyumba

ya Sirayeli ndimo ndi nyumba ya Yuda;
Si kwa kupangana komwe dinapanga ndi atatu ao 9
M' siku lomwe dinatenga awo ndi dzanja ku turutsa awo mwa dziko la Yiputa;
Kuti sanakalabe m' kupangana kwanga,
Ndimo sindinayang'anira awo, ati Mwini.
Kuti kumene kuli kupangana komwe didzapangana ndi 10
nyumba ya Sirayeli
Pambuiu masiku adya, ati Mwini;
Didzaika mau anga m' muwongo wao,
Ndimo pa ntima wao onso didzalemba awo:
Ndimo didzakala kwa awo Mulungu,
Ndimo adzakala kwa ine antu:
Ndimo sadzàpunzitsa antu onse amudzianzao, 11
Ndi antu onse abali ao, kuti, Dziwani Mwini:
Kuti onse adzadziwa ine,
Kwa ang'ono opambana kwa akuru opambana a awo.
Kuti didzakala ndi nsisi kwa mpulupulu zao, 12
Ndimo zakwaipa zao sindidzakumbukila ntawi ina.
M' tshimene anena, *Kupangana* kwatsopano, anapanga 13
koiamba kwakali. Koma kumene komwe kulikukala
kwakali, ndi kulikulitsa kwakugonera kuli pafupi kwa ku
kang'ganuka.

Ndimo inde *kupangana* koiamba kunali ndi maloezo a 9
kuimirira kwamulungu, ndimo malo oyera atshi, *malo oyera*
a dziko limene. Kuti kunafotokozedwa msasa, woiamba, 2
momwe *zinali* tshogwirira nyali, ndi gome, ndi mikate
yoonetsa; womwe utshedwa Malo Oyera. Ndimo pambuiu 3
tshopimba tshatshiwiri, msasa womwe utshedwa Woyera wa
oyera; uli ndi tshogwirira zonung'kira tshagolide, ndi arke 4
la kupangana lopatikidwa kozungulira ndi golide, momwe
*unali* mpika wagolide wosungira mana, ndi tole ya Haron
yomwe inapuka, ndi magome a kupangana; ndimo pa- 5
mwamba pa ilo makerube a kupambana kupimba mpando-
wa-nsisi; ndi zintu zomwe sitidziwa tsopano ku nena koanja-
nitswa. Koma zintu zimenezi zinafotokozedwa tshointsho, 6
adzukuru aloabe m' msasa woiamba, kuta maimiriro; koma 7
mwa watshiwiri ndzukuru wang'kuru eka, kamodzi m'
tshaka, si wopanda mwazi, womwe atsira kwa ie eka, ndi
kwa matshimo a antu: Nzimu Woyera kusonyeza tshimene, 8
kuti njira mwa malo oyera kosuntira sanasonyezedwa, ntawi
monga msasa woiamba uiikuima kosuntira; tshomwe *tshiri* 9

fanizo kwa ntawi yatsopano; kwa tshomwe zitsiridwa mitulo
ndi zinsembe zomwe zosadziwa, monga ndi kudzidziwitsa,
10 ku panga wopembedza wotetsa, *ziri* zoka (ndi zakudia ndi
kumwa ndi kutsuka kwina) maloezo anyama, oikidwa kwa
ntawi ya kupanga anso.
11 Koma Kristu anadza ndzukuru wang'kuru wa zintu
zabwino zomwe zirinkudza, mwa msasa woukuru wopa-
mbana ndi wakuta wopambana, sunamangidwa ndi
12 manja, omwe ali ku nena, si wa kupanga kumene, kapena
kosuntira si mwa mwazi wa agogo ndi ana a ng'ombe, koma
mwa mwazi watshi woka, naloa kamodzi kwa onse m' malo
13 oyera, kunalandira kuombola kosamariza. Kuti ngati
mwazi wa agogo ndi ng'ombe zampongo, ndi mapolusa a
nsoti kuwaza awo omwe anadetsedwa, ziyeretsa kwa kutsuka
14 kwa nyama: bwanje ambiri kopambana mwazi wa Kristu,
emwe mwa Nzimu wosamariza natsira ie eka wopanda
tshirama kwa Mulungu, udzatsukitsa kudzidziwitsa
kwanu kwa ntshito zakufa ku imirira Mulungu wamoyo?
15 Ndimo kwa tshifukwa tshimene ali wolekanitsa wa kupa-
ngana kwatsopano, kuti imfa inakala kwa kuombola
kwa matshimo omwe anali pansi pa kupangana koiamba,
awo omwe anaitanidwa angolandira lonjezano la kuloa
16 kosamariza. Kuti pomwe kulipo kufuna, kukanakala ndi
17 kufunidwa imfa ya ie emwe anakupanga. Kuti kufuna
kuli ndi mpamvu pomwe inali imfa: kuti ntawi ina kodi
kuli kantu ntawi ie emwe anakupanga ali ndi moyo?
18 Mwa kuti inde *kupangana* koiamba sikunasonyezedwa
19 kopanda mwazi. Kuti ntawi mau onse analankulidwa ndi
Moses kwa antu onse kwa mau, natenga mwazi wa ana a
ng'ombe ndi agogo, ndi madzi ndi wulu wofira ndi hisopi,
20 nawaza buku ilo loka, ndi antu onse, kunena, Umene uli
mwazi wa kupangana komwe Mulungu nauza kwa inu.
21 Kopambana msasa ndi dziwira dzonse dza kuimirira nawaza
22 modzimodzi ndi mwazi. Ndimo kwa mau, dingonena
pafupi, zintu zonse zitsukidwa ndi mwazi, ndimo kobaluka
kwa kuturutsa mwazi kulibe kubweza.
23 Ndimo kunali ndi kufunidwa kuti dzofaniza dza zintu m'
miamba dzikanatsukidwa ndi zimenezi; koma zintu
zamwamba izo zoka ndi zinsembe zabwino zopambana
24 zimenezi. Kuti Kristu sanaloa m' malo oyera opangidwa
ndi manja, ofana m' sonyezo kwa oona; koma m' mwamba
imo moka, tsopano ku onekera patsogolo pa nkope ya

Mulungu kwa ife: kapena kosuntira si kuti akadzitsira 25
ntawi zambiri; monga ndzukuru wang'kuru aloa m' malo
oyera tshaka ndi tshaka ndi mwazi si watshi; kani ntawi 26
zambiri akanamva kwa kuzika kwa dziko: koma tsopano
kamodzi pa nsonga ya magonero wasonyezedwa ku tshotsa
mpulupulu ndi nsembe ya ie eka. Ndimo m' monga ambiri 27
monga kuloezedwa kwa antu ku fa kamodzi, ndimo pambuiu
kumene *kudza* kuweruza; tshointsho Kristu unso, anatsi- 28
ridwa kamodzi ku nyamula zakwaipa za ambiri, adzasonyeza
ntawi yatshiwiri, wobaluka kwa mpulupulu, kwa awo omwe
alindira ie, kwa kupulumutsa.

Kuti mau ali ndi ntunzi wa *zintu* zabwino zirinkudza, si 10
fanizo nditu la zintu, ndi nsembe zimenezi tshaka ndi
tshaka, zomwe atsirabe, palibe ntawi osadziwa ku panga
akuta awo omwe ayandika. Kani kodi zikanaleka ku 2
tsiridwa, tshifuka opembedza, anatsukidwa kamodzi, saka-
napotshera ntawi ina kudzidziwitsa kwa zimpulupulu?
Koma m' *nsembe* zidya kuli kukumbutsa kupangidwa kwa 3
zimpulupulu tshaka ndi tshaka. Kuti kuli kusadziwa ku ta 4
kuti mwazi wa ng'ombe zampongo ndi agogo ukatshotsa
zimpulupulu. Mwa kuti ntawi afika m' dziko, ati, 5

Nsembe ndi tshopatsa usanafuna,
Koma tupi unafotokoza kwa ine;
M' zopatsa zootshedwa zatuntu ndi *zinsembe* kwa mpu- 6
lupulu usanapotshera kusekera:
Pomwe dinati, Ona, dafika 7
(M' mputu wa buku kulembedwa ndi ine)
Ku tshita kufuna kwako, Ō Mulungu.

Kunena poiamba, Zinsembe ndi zopatsa ndi zopatsa zoo- 8
tshedwa zatuntu ndi *zinsembe* kwa mpulupulu usanafuna,
kapena usanapotshera kusekera mwa izo (zomwe zitsiridwa
kwa mau), pomwe wanena, Ona, dafika ku tshita kufuna 9
kwako. Atshotsa koiamba, kuti angolimbikitsa kwa-
tshiwiri. Ndi kufuna komwe tayeretsedwa mwa tshopatsa 10
tsha tupi la Yesu Kristu kamodzi kwa onse. Ndimo adzu- 11
kuru onse nditu aima siku ndi siku kuimirira ndi ku tsira
ntawi zambiri nsembe zimenezi, zomwe zosadziwa ntawi ina
ku tshotsa zimpulupulu: koma ie, ntawi anatsira nsembe 12
imodzi kwa zimpulupulu kwa ntawi yonse, nakala pansi pa
dzanja lamanja la Mulungu; kwa ntawi yatsopano kuya- 13
ng'anira kwa ntawi maliwongo atshi apangidwa mpando wa
mapazi atshi. Kuti ndi tshopatsa tshimodzi watetsa kwa 14

15 ntawi yonse awo omwe ayeretsedwa. Ndimo Nzimu
Woyera anso umariza ndi ife: kuti pambuiu wanena,

16 Kumene kuli kupangana komwe didzapangana ndi awo
Pambuiu masiku adya, ati Mwini;
Didzaika mau anga pa ntima wao,
Ndimo pa muwongo wao onso didzalemba awo;

*pomwe ati*,

17 Ndimo zakwaipa zao ndi mpulupulu zao sindikumbukila ntawi ina.

18 Koma pomwe kuli kubweza kwa zimenezi, kusali ntawi ina
tshopatsa kwa mpulupulu.
19 Ndimo kupotshera, abali, kulimbika ku loa m' malo
20 oyera ndi mwazi wa Yesu, ndi njira yomwe nasonyeza kwa
ife, njira yatsopano ndi yamoyo, mwa tshopimba, tshomwe
21 tshiri ku nena, nyama yatshi; ndimo *kupotshera* ndzukuru
22 wang'kuru pa nyumba ya Mulungu; tiyandike ndi ntima
woona m' kudzaza kwa mvanu, kupotshera mitima
yatu yowazidwa kwa kudzidziwitsa koipa, ndi tupi latu
23 lotsukidwa ndi madzi oyera: tigwire kolimba kubvomereza
kwa kulingalira kwatu kuti kusagwedera; kuti ie ali
24 wamvanu emwe nalonjezana: ndimo tiganizane ku bvutana
25 kwa kukonda ndi ntshito zabwino; sikulekana kusong'kana
kwa ife toka, monga ntengo wa ena uli, koma kutaulira
*modzi ndi wina;* ndimo kwambiri kopambana, monga muona
siku liyandika.
26 Kuti ngati titshimwa ndi kufuna kwatu pambuiu kuti
talandira kudziwa kwa nteradi, kusatsala ntawi ina nsembe
27 kwa zimpulupulu, koma kuyang'anira kwina koopsa kwa
kuweruza, ndi ukali wa moto womwe udzamwaza maliwongo.
28 Muntu emwe wanyoza mau a Moses afa wopanda nsoni pa
29 *mau a* omariza awiri kapena atatu: ndi kulanga kolimba
kwambiri kopambana, muganiza bwanje, ie adzaganizidwa
woenera, emwe wapondereza Mwana wa Mulungu, ndimo
wawerenga mwazi wa kupangana, ndi womwe anayeretsedwa,
tshintu tshanko, ndimo wanyoza Nzimu wa kufatsa?
30 Kuti tidziwa ie emwe nanena, Kuzimbula kuli kwa ine,
didzalipira. Ndimo onso, Mwini adzaweruza antu atshi.
31 Tshiri tshintu tshoopsa ku gwa m' manja a Mulungu wamoyo.
32 Koma kumbutsani masiku akali, mwa omwe, pambuiu
munaunikidwa, munamvabe kumenyana kwakukuru kwa
33 kumva; kwina, kunapangidwa tshoyang'anira ndimo ndi

masinjiriro ndi masautso; ndimo kwina, kukala ogawana
ndi awo omwe anatshitidwa tshointsho. Kuti munamva 34
tshisoni pa awo omwe anali m' zomangira, ndimo muna-
landira kosekera kuononga kwa zintu zanu, kudziwa kuti
inu noka muli ndi kupotshera kwabwino kopambana ndimo
kokalabe. Ndimo musataia kulimbika kwanu, komwe 35
kupotshera kulipira kwakukuru kwa kusekeretsa. Kuti 36
muli ndi kufunidwa kwa kulongosola, kuti, munatshita
kufuna kwa Mulungu, mungolandira lonjezano.

Kuti kosuntira ntawi yeing'ono nditu, 37
Ie emwe afika adzafika, ndimo sadzakala.
Koma wodeka wanga adzakala ndi moyo ndi mvanu: 38
Ndimo ngati adzizing'ka, nzimu wanga suli ndi
kusekera mwa ie.

Koma sitiri a omwe adzizing'ka kwa kumwaza; koma a 39
awo omwe ali ndi mvanu kwa kupulumutsa kwa nzimu.

Koma mvanu uli kulimbika kwa *zintu* zolingaliridwa, 11
kuyesa kwa zintu zosaonekedwa. Kuti mwa iwo akuru 2
anamarizidwa nao. Ndi mvanu didziwitsa kuti magonero 3
analumukizidwa ndi mau a Mulungu, monga kuti tshomwe
tshionedwa sitshinapangidwa ndi zintu zomwe zionekera.
Ndi mvanu Habeli natsira kwa Mulungu nsembe yabwino 4
yopambana Kayin, mwa yomwe anamarizidwa nai' kuti
anali wodeka, Mulungu kumariza ndi mitulo yatshi: ndimo
mwa iwo ie anafa kosuntira alankula. Ndi mvanu Henoke 5
wasuntidwa kuti sakanaona imfa; ndimo sanapezedwa,
tshifuka Mulungu nasunta ie: kuti patsogolo pa kusunta
kwatshi wamarizidwa nai', kuti anakala wosekeretsa bwino
kwa Mulungu: ndimo wopanda mvanu kuli kusadziwa ku ta 6
ku sekeretsa bwino *ie:* kuti ie emwe afika kwa Mulungu
akanamvana kuti ali, ndi *kuti* ali wolipira wa awo omwe
afuna pambuiu pa ie. Ndi mvanu Nowa, kunaambiriridwa 7
*ndi Mulungu* kwa zintu sizoonekera monga kosuntira,
nafulumizidwa ndi kuopa kopembedza, nafotokoza arke
kwa kupulumutsa kwa nyumba yatshi; mwa womwe
nasautsa dziko, nakala woloa wa kudeka komwe kuli kwa
mvanu. Ndi mvanu Abraham, ntawi anaitanidwa, namvera 8
ku turuka kwa malo omwe analikulandira kwa zoloa;
ndimo naturuka, sanadziwa kuti namuka. Ndi mvanu 9
nakala waulendo m' dziko la lonjezano, monga m' *dziko* si
latshi, kukala m' misasa, ndi Yisake ndi Yakobe, oloa ndi ie
a lonjezano lomwe: kuti nayang'anira mzinda womwe uli 10

ndi maziko, womanga ndi wopanga wa womwe ali Mulungu.
11 Ndi mvanu inde Sara ie eka nalandira mpamvu ku bvuuka
mbeu ntawi anali wopambana kugonera, tshifuka naganiza ie
12 wamvanu emwe analonjezana: mwa kuti inso nauka kwa
modzi, ndi ie wofana ndi wakufa, *tshointsho ambiri* monga
nyenyezi za mwamba m' kutshuruka, ndimo monga ntshenga,
womwe uli ku doko, wosawerengedwa.
13 Amene onse anafa m' mvanu, sikunalandira malonjezano,
koma anaona awo nautsa awo kwa kutali, ndimo anabvome-
14 reza kuti anali aulendo ndi alendo pa dziko. Kuti awo
omwe anena zintu zotere asonyeza kuti alikufuna dziko la
15 awo oka. Ndimo ngati nditu anakumbukila ndi *dziko*
limene kwa lomwe naturuka, akanapotshera pofatsa ku
16 bwera. Koma tsopano afuna *dziko* labwino lopambana,
lomwe liri, lakumwamba: mwa kuti Mulungu siali ndi
manyazi ndi awo, kutshedwa Mulungu wao: kuti wafotokoza
mzinda kwa awo.
17 Ndi mvanu Abraham, anayesedwa, anatsira Yisake: inde,
ie emwe analandira malonjezano kosekera analikutsira
18 *mwana* watshi wobadwa eka; *inde ie* kwa emwe analanku-
19 lidwa, M' Yisake mbeu yako idzaitanidwa: kuganiza kuti
Mulungu *ali* ndi mpamvu ku ukitsa, inde kwa akufa; kwa
20 uko onso m' fanizo analandira ie enso. Ndi mvanu Yisake
21 nadalitsa Yakobi ndi Esau, inde ndi zintu zirinkudza. Ndi
mvanu Yakobi, ntawi anatofuna ku fa, nadalitsa onse a ana
a Yosefe; napembedza, *kutshirikiza* pamwamba pa ndodo
22 yatshi. Ndi mvanu Yosefe, ntawi nsonga yatshi inali pafupi,
natshula ndi kutshoka kwa ana a Sirayeli; napatsa mau ndi
23 mafupa atshi. Ndi mvanu Moses, ntawi anabadwa, anabisi-
dwa miezi itatu ndi atatu atshi ndi amai atshi, tshifuka
naona anali mwana wabwino; ndimo sanaopa mau a fumu
24 yotshuka. Ndi mvanu Moses, ntawi anakula, nakana ku
25 tshedwa mwana wa mwana wankazi wa Faro; kusang'ka ku
ipidwa ndi antu a Mulungu, kopambana ku kondwera masekero
26 a mpulupulu kwa nsiku; kuganiza sinjiriro la Kristu zolemera
zazikuru zopambana zolemera za Yiputa: kuti nayang'anira
27 kwa kulipira kwa sekeretso. Ndi mvanu nasia Yiputa,
sikuopa kukwiira kwa fumu yotshuka: kuti anamvabe,
28 monga kuona ie emwe ali wosaonekedwa. Ndi mvanu
wapanga mpasika, ndi kuwaza kwa mwazi, kuti womwaza
29 wa obadwa oiamba sakatosa awo. Ndi mvanu napita mwa
Nyanja Yofira monga ndi ntunda wouma: komwe Ayiputa

anayesa ku tshita anamezedwa. Ndi mvanu makoma a 30
Yeriko anagwa, pambuiu nazungunizidwa kwa masiku asanu
ndi awiri. Ndi mvanu Rahabi nkazi wa dama sanamwazika 31
ndi awo omwe anali osamvera, analandira zinzondi ndi
ntendere. Ndimo tshiani didzanena kopambana? kuti 32
ntawi idzapereweza ine ngati diuza ndi Gidyon, Baraki,
Samson, Yefta; ndi Davide ndi Samuweli, ndi aprofeti:
omwe mwa mvanu napondereza maiko, natshita kudeka, 33
nalandira malonjezano, natseka nkamwa mwa mikango,
nazima mpamvu ya moto, napulumuka kukutwa kwa 34
mpeni wa nkondo, kwa kufoka anapangidwa olimba,
nakula olimba m' nkondo, natamangitsa magulu a ankhondo
a dziko lina. Akazi nalandira akufa ao ndi kuukirira: ndi 35
ena anasautsidwa, sikulandira kumasula kwao; kuti anango-
landira kuukirira kwabwino kopambana: ndimo ena 36
anapotshera kuyesa kwa matonzo ndi makwapulo, inde,
kopambana kwa zomangira ndi kuikidwa m' nyumba ya
ndima: anaponyedwa ndi miala, anatshekedwa kolekanitsa, 37
anayesedwa, anapedwa ndi mpeni wa nkondo: naendaenda
m' dzikopa dza nkosa, m' dzikopa dza agogo; anali osauka,
osautswa, oipidwa (ndi omwe dziko lisanaenera), kusotshera 38
m' dzipululu ndi mapiri ndi mapanga, ndi mauna a dziko.
Ndimo amene onse, anamarizidwa ndi awo mwa mvanu wao, 39
sanalandira lonjezano, Mulungu anakwanitsa tshintu tshina 40
tshabwino tshopambana kwa ife, kuti obaluka kwa ife
sakatetsedwa.

Ndimo onso, kuona tizungunizidwa ndi ntambo woukuru 12
wotere wa omariza, tiike pansi zolemedwa zonse, ndi tshimo
lomwe lizerenga ife, ndimo titamange ndi kulongosola liwiro
lomwe liikidwa patsogolo pa ife, kuyang'anira kwa Yesu 2
Woiamba ndi Wakuta wa mvanu *watu*, emwe kwa tshimwe-
mwe tshomwe tshinaikidwa patsogolo pa ie anamvabe
nkhwitshi, kunyoza manyazi, ndimo wakala pansi pa dzanja
lamanja la mpando wotshuka wa Mulungu. Kuti ganiza ie 3
emwe wamvabe nseke wotere wa ampulupulu pa awo oka,
kuti musakula olema, kufoka m' mizimu yanu. Kosuntira 4
simunakana kwa mwazi, kumenyana pandunji pa mpulupulu:
ndimo mwaiwala kutaulira, komwe kuganizirana ndi inu 5
monga ndi ana,

Mwana wanga, usayang'anira kopeputsa kulanga kwa
Mwini,
Kapena usafoka ntawi usuiumulidwa ndi ie;

6 Kuti emwe Mwini akonda alanga,
Nakwapula ana onse omwe alandira.
7 Kuli kwa kulanga kuti mumvabe; Mulungu atshita ndi
inu monga ndi ana; kuti mwana wanje alipo emwe atatu
8 *atshi* wosalanga? Koma ngati muli opanda kulanga, ndi
komwe onse anapangidwa ogawana, pomwe muli ana a
9 mtengo, ndimo si ana. Kopambana, tinali ndi atate a nyama
yatu ku langa ife, ndimo tinapatsa awo kudzinga: kodi
kwambiri kopambana tidzakala pansi pa Atate a mizimu,
10 ndimo tikala ndi moyo? Kuti awo nditu kwa masiku
owereng'jeka nalanga *ife* monga kunaenedwa bwino ku awo;
koma ie kwa kupindulidwa *kwatu*, kuti *ti*ngokala ogawana a
11 kuyera kwatshi. Kulanga konse kuenedwa kwa tsopano
ku li si kwatshimwemwe, koma kolemera: kosuntira pambuiu
kubala tshobala tshantendere kwa awo omwe anadzitshitidwa
12 ndi komwe, *inde tshobala* tsha kudeka. Mwa kuti tukulani
13 manja omwe awerama, ndi maondo adzanzi; ndimo pangani
njira zolungama kwa mapazi anu, kuti kumene komwe kuli
kopunduka kusatshotsedwa kwa njira, koma kopambana ku
tshiritsidwa.
14 Tsatani pambuiu pa ntendere ndi antu onse, ndimo kuye-
retsedwa kopanda komwe palibe muntu adzaona Mwini:
15 kuyang'anira kotshenjera kani *alipo* muntu modzi emwe
apereweza ndi kufatsa kwa Mulungu; kani ntsitsi wina wa
kuawa kumera ubvuta *inu*, ndi komwe ambiri adetsedwa;
16 kani *alipo* wadama modzi, kapena modzi wanko, monga Esau,
emwe kwa ntanda wa kudia nagulitsa kwatshi kwa kubadwa.
17 Kuti mudziwa kuti inde ntawi pambuiu nafuna ku loa m'
dalo, nataiidwa (kuti sanapeza malo a kutembenuza ntima),
ngati naafuna kwatshangu ndi misozi.
18 Kuti simunafika kwa *piri* lomwe linangotosedwa, ndi
lomwe linaotshedwa ndi moto, ndi kwa kudetsa, ndi ndima,
19 ndi mondwe, ndi liu la lipenga, ndi liu la mau; lomwe awo
omwe anamva napempa kuti palibe mau ena akanenedwa
20 kwa awo: kuti sanadziwa ku mvabe omwe anauzidwa,
21 Ngati inde nyama itosa piri, idzaponyedwa miala; ndimo
tshoopsa tshotere tshinali tshoonekera, *kuti* Moses nati,
22 Diopa kwambiri ndintuntumira: koma munafika kwa piri
la Ziyon, ndimo kwa mzinda wa Mulungu wamoyo,
Yerusalem wamwamba, ndi kwa magulu osawerengedwa a
23 anjelo, kwa kusong'kana kwa onse, ndi eklesia la obadwa
oiamba omwe alembedwa m' mwamba, ndimo ku Mulungu

Woweruza wa onse, ndi ku mizimu ya antu odeka inatetse-
dwa, ndimo ku Yesu wolekanitsa wa kupangana kwatsopano, 24
ndimo kwa mwazi wa kuwaza womwe ulankula bwino
kopambana *ndi womwe wa* Habeli. Onani kuti musakana 25
ie emwe alankula. Kuti ngati awo sanapulumuka, ntawi
anakana ie emwe anatshenjeza *awo* pansi, kwambiri kopa-
mbana *sitidzapulumuka*, tomwe titembenuka kwa ie emwe
*atshenjeza* kwa kumwamba: liu la emwe pomwe linagwedesa 26
dziko: koma tsopano walonjezana, kuti, Kosuntira ntawi
ina didzapanga ku ntuntumira si dziko loka, koma anso
kumwamba. Ndimo *mau* amene, Kosuntira ntawi ina, asonye- 27
za kusunta kwa zintu zomwe zigwedezedwa, monga kwa
zintu zomwe zinapangidwa, kuti zintu zidya zomwe sizigwe-
dezedwa zingokala. Mwa kuti, kulandira dziko lomwe 28
losadziwa ku gwedezedwa, tipotshere kufatsa, ndi komwe
tingotsira kuimirira kosekeretsa bwino kwa Mulungu
ndi kudzinga ndi kuopa: kuti Mulungu watu ali moto 29
wonyeka.

Kukonda kwa abali kukalebe. Musaiwala ku sonya 13
kukonda kwa alendo: kuti ndi kumene ena anasungira
anjelo kosadziwika. Kumbukilani awo omwe ali m' zoma- 3
ngira, monga omangidwa ndi awo; awo omwe aipidwa,
monga muli inu noka anso m' tupi. Kukwata *kukale* ndi 4
ulemu mwa onse, ndimo mpasa *ikale* yosadetsedwa: kuti
adama ndi atshigololo Mulungu adzaweruza. Kalani aufulu 5
kwa kukonda kwa zindrama; osekera ndi zintu zotere
monga mupotshera: kuti ie eka wati, Sindidzapereweza iwe
m' kantu, kapena sindidzasia iwe m' kantu. Tshointsho 6
kuti ndi kulimba ntima bwino tinena,

Mwini ali wotangata wanga; sindidzaopa:
Tshiani muntu adzatshita kwa ine?

Kumbukilani awo omwe anali ndi kuweruza pa inu, 7
omwe analankula ndi inu mau a Mulungu; ndimo kuganiza
makalidwe a moyo wao, fanizirani mvanu wao. Yesu 8
Kristu *ali* modzimodzi dzulo ndi lero, *inde* ndi kwa
magonero. Musanyamulidwa ndi mapunzitso ena ndi 9
osadziwidwa: kuti tshiri tshabwino kuti ntima ulimbiki-
tsidwa ndi kufatsa; si ndi zakudia, m' zomwe awo omwe
anaendaenda sanapindulidwa. Tiri ndi katshisi, ndi emwe 10
awo alibe kwao ku dia omwe aimirira msasa. Kuti matupi 11
a nyama zidya, mwazi wa zomwe utengedwa m' malo oyera
ndi ndzukuru wang'kuru *monga tshotsira* kwa mpulupulu,

12 aotshedwa kunja kwa tsasa. Mwa kuti Yesu unso, kuti
anangoyeretsa antu mwa mwazi watshi, namva kunja kwa
13 tshipata. Ndimo tituruke kwa ie kunja kwa tsasa, kunya-
14 mula sinjiriro latshi. Kuti sitipotshera pano mzinda
wokalabe, koma tifuna kwa *mzinda* womwe ulinkudza.
15 Mwa ie pomwe titsire nsembe ya kulemekeza kwa Mulungu
ntawi yonse, kuli, tshobala tsha milomo yomwe ibvomereza
16 dzina latshi. Koma ku tshita bwino ndi ku gawaniza musa-
iwala: kuti ndi nsembe zotere Mulungu asekera bwino.
17 Mverani awo omwe ali ndi kuweruza pa inu, ndimo lolani
*awo;* kuti adikira kwa mizimu yanu, monga awo omwe
adzawerengera; kuti angotshita kumene ndi tshimwemwe,
ndimo si ndi tshisoni: kuti kumene *kunali* kosapindulidwa
kwa inu.
18 Pemperani kwa ife: kuti tikantshiziridwa kuti tipotshera
kudzidziwitsa kwabwino, kufuna kukala kwape ndi moyo m'
19 zintu zonse. Ndimo ditaulira *inu* kwambiri kopambana ku
tshita kumene, kuti dingobwezedwa kwa inu nsanga yopa-
mbana.
20 Koma Mulungu wa ntendere, emwe natenga anso kwa
akufa mbusa wang'kuru wa nkosa ndi mwazi wa kupangana
21 kosamariza, *inde* Mwini watu Yesu, atetse inu m' zintu
zonse zabwino ku tshita kufuna kwatshi, kutshita mwa ife
tshimene tshomwe tshisekeretsa bwino m' kuona kwatshi,
mwa Yesu Kristu; kwa emwe *kuli* kupambana kwa magonero
a magonero. Amen.
22 Koma ditaulira inu, abali, imvani ndi mau a kutaulira:
23 kuti dalemba kwa inu m' mau owereng'jeka. Dziwani kuti
mbali watu Timote wamasulidwa; ndi emwe, ngati afika
m' ntawi yeing'ono, didzaona inu.
24 Utsani awo onse omwe ali ndi kuweruza pa inu, ndi oyera
onse. Awo a Yitaliya autsa inu.
25 Kufatsa kukale ndi inu nonse. Amen.

EPISTOLA LA

# YAKOBI.

YAKOBI, kapolo wa Mulungu ndi wa Mwini Yesu 1
Kristu, kwa mafuko kumi ndi awiri omwe ali a
Kubalalika, kuyankula.

Ganiza tshonse tshimwemwe, abali anga, ntawi mugwa m' 2
mayeso ena; kudziwa kuti kuyesera kwa mvanu wanu 3
kutshita kulongosola. Ndimo kulongosola kukale ndi 4
ntshito *yatshi* yakuta, monga kuti mungokala akuta ndi
otshikalire, kusapanda m' kantu

Koma ngati modzi wa inu apanda nzeru, afunse Mulungu, 5
emwe apatsa ku onse kwaufulu ndi wosatonza; ndimo
zidzapatsidwa kwa ie. Koma apempe ndi mvanu, wosakaika 6
kantu: kuti emwe akaika ali wofana ndi funde la nyanja
lipiswa ndi mpepo ndi ku ponyedwa. Kuti muntu amene 7
asaganize kuti adzalandira kantu kwa Mwini; muntu wa 8
mauwongo awiri, wosakazizika m' njira zatshi zonse.

Koma mbali watshabe apambane m' ukulu watshi: 9
ndi wolemera, m' tshimene kuti apangidwa tshabe: tshifuka 10
kuti monga lua la udzu adzapita. Kuti dzua lituruka ndi 11
mpepo yakwinyatitsa, ndimo liumitsa maudzu; ndimo lua
latshi ligwa, ndi kukoma kwa makalidwe atshi kumwaza:
tshointsho onso muntu wolemera adzasonyala m' maulendo
atshi.

Wodala ali muntu emwe amvabe tshinyengo: kuti ntawi 12
anali woyesedwa, adzalandira tshisoti tshotshuka tsha moyo,
tshomwe *Mwini* analonjezana ku awo omwe akonda ie.
Palibe muntu anene ntawi anyengedwa, Dinyengedwa ndi 13
Mulungu: kuti Mulungu wosadziwa ku nyengedwa ndi
mpulupulu, ndimo ie eka wosanyenga muntu: koma antu 14
onse anyengedwa, ntawi akokedwa ndi kufuna kwao, ndi ku
nyenjeredwa. Ndimo kufuna, ntawi kwinabvuuka, kwibala 15
mpulupulu: ndimo mpulupulu, ntawi ikula, ibala imfa.
Musanyengedwa, abali anga okondedwa. Zaulere zabwino 16,17
zonse ndi zokwanira zonse zakuta ziri za kumwamba,
zitsika kwa Atate a miune, ndi emwe kulibe kudziwa ku

kala kupendukapenduka, kapena ntunzi womwe uikidwa ndi
18 kutembenuka. Ndi kufuna kwatshi koka nabala ife ndi mau
a nteradi, kuti tikakala mtundu wa dzobala dzoiamba dza
zopanga zatshi.
19 Mudziwa *tshimene*, abali anga okondedwa. Koma antu
onse akale aliwiro ku mva, ododoma ku lankula,
20 ododoma kwa kukwiira: kuti kukwiira kwa muntu
21 kusatshita kudeka kwa Mulungu. Ndimo kutshotsa
kunyansa konse ndi kugabvikira kwa mpulupulu, landirani
ndi kuanja mau ookedwa, omwe ali ndi mpamvu ku pulu-
22 mutsa mizimu yanu. Koma kalani otshita a mau, ndimo si
23 omva oka, kudzinyenga inu noka. Kuti ngati modzi ali
womva wa mau, ndimo si*ali* wotshita, ali wofana ndi muntu
24 kuyang'ana nkope yatupi latshi m' karirole: kuti adziona,
ndimo amuka, ndimo tsopano lino aiwala muntu wanje anali.
25 Koma ie emwe ayang'ana m' mau akuta, *mau* a ufulu, na-
kala *tshointsho*, kuli si womva emwe aiwala, koma wotshita
emwe atshita, muntu amene adzadalitsidwa m' kutshita
26 kwatshi. Ngati modzi adziganiza ali wopembedza, ntawi
wosakola lilume latshi koma anyenga ntima watshi, kupe-
27 mbedza kwa muntu amene kuli kwatshabe. Kupembedza
koyera ndi kosadetsa patsogolo pa Mulungu watu ndi Atate
kuli kumene, ku tsheza ndi opanda atatu ao, ndi amasie m'
sautso yao, *ndi* ku dzisunga wosatshita manga kwa dziko.
2 Abali anga, musakala ndi mvanu wa Mwini watu Yesu
2 Kristu, *Mwini* wa kupambana, ndi tsang'ko. Kuti ngati
aloa m' sinagoge lanu muntu ndi mpete ya golide, m' nsaru
yabwino, ndimo onso aloa muntu wosauka m' nsaru yoipa;
3 ndimo musankula ndi ie emwe abvala nsaru yabwino, ndimo
muti, Kala pano m' malo abwino; ndimo munena ndi muntu
wosauka, Ima uko, kapena kala pansi pa mpando wa mapazi
4 wanga; kodi simusankula mwa inu noka, ndimo mukala
5 oweruza ndi maganizo oipa? Imvani, abali anga okonde-
dwa; kodi Mulungu sanasang'ka awo omwe ali osauka ndi
dziko, *ku kala* olemera ndi mvanu, ndi oloa a dziko lomwe
6 analonjezana kwa omwe akonda ie? Koma munapyapyaza
muntu wosauka. Kodi olemera sasautsa inu, ndi awo oka
7 akoka inu patsogolo pa amirandu? Kodi satukwana dzina
8 laulemu linatshedwa pa inu? Koma ngati mudzaza mau
ofumu, ofana ndi lemba, Udzakonda woiandikila wako monga
9 iwe eka, mutshita bwino: koma ngati muli ndi tsang'ko,
mutshita mpulupulu, mutshimikidwa ndi mau monga

otshimwa. Kuti emwe adzasunga mau onse, ndimo adza- 10
tshimwa ndi *tshintu* tshimodzi, akala wotshimwa ndi onse.
Kuti ie emwe nati, Usatshita tshigololo, nati inso, Usapa. 11
Ndimo ngati usatshita tshigololo, koma upa, ukala wotshimwa
wa mau. Tshointshi mulankula, ndi tshointshi mutshita, 12
monga antu omwe adzaweruzidwa ndi mau a ufulu. Kuti 13
kuweruza *kuli* kopanda nsisi kwa ie emwe wosasonyeza
nsisi: nsisi ipambana pa kuweruza.

Tshiani tshipindula, abali anga, ngati muntu anena ali 14
ndi mvanu, koma wosali ndi zintshito? kodi mvanu umene
udziwa ku pulumutsa ie? Ngati mbali kapena mlongo 15
ali womariseke, ndimo ali wopanda kudia kwalero, ndimo 16
modzi wa inu anena ndi awo, Endani ndi ntendere, kalani
otentedwa ndi okutitswa; ndimo kosuntira musapatsa awo
zintu zomwe zifunidwa ndi tupi; tshiani tshipindula?
Inde tshointsho mvanu, ngati usali ndi zintshito, uli wakufa 17
mwa iwo woka. Inde, muntu adzanena, Uli ndi mvanu, 18
ndimo diri ndi zintshito: sonyeza ine mvanu wako wole-
kana ntshito *zako*, ndimo ine ndi ntshito zanga didzasonyeza
iwe mvanu *wanga*. Umvana kuti Mulungu ali modzi; 19
utshita bwino: ademon anso amvana, nantentemera.
Koma kodi udzafuna ku dziwa, O muntu wodzitama, kuti 20
mvanu wolekana kwa zintshito ulitsala? Kodi Abraham 21
atatu atu sanadeketsedwa ndi zintshito, mwa tshidya natsira
Yisake mwana watshi pa katshisi? Uona kuti mvanu 22
unatshita ndi ntshito zatshi, ndimo ndi zintshito mvanu
wapangidwa wakuta; ndimo lemba linadzazidwa lomwe 23
linena, Ndi Abraham namvana ndi Mulungu, ndimo kuna-
werengedwa kwa ie kwa kudeka; ndimo natshedwa mbali
wa Mulungu. Muona kuti ndi zintshito muntu adeketsedwa, 24
ndimo si ndi mvanu woka. Ndimo tshointshi inso kodi Ra- 25
habe nkazi wa tshigololo sanadeketsedwa ndi zintshito, mwa
tshidya nalandira mitenga, natumiza awo pa njira ina?
Kuti monga tupi lolekana kwa nzimu liri lakufa, inde tshoi- 26
ntsho mvanu ulekana ndi zintshito uli wakufa.

Musakala ampunzitsi ambiri, abali anga, kudziwa kuti 3
tidzalandira kuweruza kwakukuru kopambana. Kuti m' 2
zintu zambiri tipuntwa tonse. Ngati modzi wosapuntwa
m' mau, emwe ali muntu wakuta, ali ndi mpamvu ku kola
tupi lonse enso. Ndimo ngati tiika makwerekwere a 3
akavalo m' nkamwa mwao, kuti angomvera ife, titembenuza
tupi lao lonse enso. Ona, dzombo onso, monga dziri 4

dzadzikuru dzotere, ndimo dzisuntidwa ndi mpepo zolimba,
dzitembenuzidwa ndi tsigiro laling'ono nditu, pomwe tintu
5 la woongolera lifuna. Tshointsho onso lilume liri tshiwalo
tshatshing'ono, ndimo lidzitama zintu zazikuru. Ona,
bwanje mtengo lalikuru liatswa ndi kamoto kakang'ono
6 bwanje! Ndimo lilume liri moto: dziko la mpulupulu
mwa dziwalo dzatu liri lilume, lomwe lidetsa tupi lonse,
ndimo liatsa hwile la makalidwe, ndi liatsidwa ndi geena.
7 Kuti mitundu yonse ya nyama ndi ya mbalame, ndi ya
zokwawa ndi zintu m' nyanja, zizoloweredwa, ndimo zazo-
8 loweredwa ndi antu: koma lilume palibe muntu adziwa
ku zolowera; *liri* kuipa kosapuma, *liri* lodzaza ndi ma-
9 nkwala akupa nditu. Ndi limene tidalitsa Mwini ndi
Atate; ndi limene titukwana antu, omwe apangidwa mwa
10 makalidwe a Mulungu: mwa nkamwa momwe zituruka
kudalitsa ndi kutukwana. Abali anga, zintu zimenezi
11 zosakanakala tshointsho. Kodi kasope aturutsa pa mpanda
12 imodzi *madzi* otsetshemera ndi oawa? kodi ntengo wa
nkuyu, abali anga, udziwa ku bala maolive, kapena mvina
zinkhuyu? kapena madzi antshere *osadziwa* ku kala
otsetshemera.
13 Ndani ali ndi nzeru ndi kudziwa mwa inu? asonyeze
ndi moyo watshi wabwino ntshito zatshi mwa kufatsa kwa
14 nzeru. Koma ngati muli ndi nsanje yakuawa ndi kuga-
wana mwa ntima wanu, musapambana ndimo musanama
15 pa nteradi. Nzeru zimene siziri *nzeru* zomwe zitsika kwa
16 kumwamba, koma ziri zapansi, zatupi, zademon. Kuti
pomwe nsanje ndi kugawana ziripo, ziri kusokanikila ndi
17 ntshito zonse zoipa. Koma nzeru zomwe ziri kwa ku-
mwamba ziri zoiamba zoyera, ndimo zantendere, zaulere,
zabvomereza kopepuka, zodzaza ndi nsisi ndi dzobala
dzabwino, zopanda kuganizaganiza, zopanda tshinyengo.
18 Ndimo dzobala dza kudeka dzifesedwa mwa ntendere ndi
awo omwe apanga ntendere.
4 Nkondo *zidzera* kuti ndi ndeu *zidzera* kuti mwa inu?
kodi *sizidzera* komwe, *inde* kwa zosekera zanu zomwe
2 zipanga nkondo mwa dziwalo dzanu? Mufuna, ndimo
musapotshera: mupa, ndimo musirira, ndi musadziwa ku
landira: mumenyana ndi mupanga nkondo; musapotshera,
3 tshifuka kuti simufunsa. Mufunsa, ndi musalandira,
tshifuka kuti mufunsa koipa, kuti mungogulitsa pa masekero
4 anu. Inu akazi a tshigololo, kodi musadziwa kuti bwenzi

la dziko liri kudana ndi Mulungu? Ndimo emwe afuna
ku kala mbali wa dziko adzipanga liwongo la Mulungu.
Kapena kodi muganiza kuti lemba linena kwa tshabe? 5
Kodi nzimu womwe napanga ku kala mwa ife ufunitsa kwa
kudana? Koma apatsa kufatsa kopambana. Ndimo 6
*lemba* linena, Mulungu akaniza odzitama, koma apatsa ku-
fatsa kwa osadzitama. Ndimo kalani pansi pa Mulungu; 7
koma kaniza diabolos, ndimo adzatawa kwa inu. Yandi- 8
kani kwa Mulungu, ndimo adzayandika kwa inu. Sambani
manja anu, ampulupulu; ndimo konzetsani mitima yanu,
osakazizika. Sautsidwani, ndimo lirani, ndimo lirani nsozi: 9
kuseka kwanu kutembenuzidwe kwa kulira, ndi tshimwe-
mwe tshanu kwa tsholemera. Dzitshepetseni m' kuona 10
kwa Mwini, ndimo adzapambanitsa inu.

Musalankula pa wina ndi wina, abali. Emwe alankula 11
pa mbali, kapena aweruza mbali watshi, alankula pa mau,
naweruza mau: koma ngati uweruza mau, uli si wotshita
wa mau, koma woweruza. Modzi *eka* ali wopatsa-mau ndi 12
woweruza, *inde* iemwe ali ndi mpamvu ku pulumutsa ndi
ku mwaza: koma uli ani emwe uweruza woiandikila wako?

Nanga anso, inu nomwe munena, Lero kapena mawa 13
tidzamuka m' zinda umene, ndimo tidzakala umo tshaka
tshimodzi, ndimo tidzagula, ndimo tidzapindula: ntawi 14
monga musadziwa tshomwe tshidzakala pa mawa. Moyo
wanu uli tshiani? Kuti muli mpwea, womwe usonyeza kwa
ntawi yeing'ono, ndimo ukanganuka. Kwa amene mukana- 15
nena, Ngati Mwini afuna, tidzakala ndi moyo, ndimo titshita
tshimenetshi kapena tshimene tshidya. Koma tsopano mu- 16
pambana m' kudzitama kwanu: kupambana konse kotere
kuli koipa. Ndimo kwa ie emwe adziwa ku tshita ubwino, 17
ndimo wosautshita, kwa ie iri mpulupulu.

Nanga anso, inu olemera, lirani nsozi ndi ku pfula kwa 5
zisoni zanu zomwe zirinkudza pa inu. Zolemera zanu ziri 2
zobvunda, ndi maraia anu ali odibwa ndi tshikululu. Golide 3
zanu ndi silivere zanu ziri ndi dzimbiri; ndimo dzimbiri
dzazo dzidzakala kwa kumariza pa inu, ndimo dzidzadia
nyama yanu monga moto. Munaika zolemera zanu m'
masiku akutungo. Ona, kulipira kwa otshita omwe anatema 4
minda yanu, komwe kubwezedwa ndi tshinyengo ndi inu,
kupfula: ndi mapfulo a omwe anatema mwaloa m' makutu
a Mwini wa Magulu a ankhondo. Munadierera pa dziko, 5
ndimo munatenga kusekera kwanu; munalera mitima yanu

6 m' siku la kupa. Munasutsa, munapa wodeka; wosakaniza
inu.
7 Ndimo kalani olongosoka, abali, kwa kudza kwa Mwini.
Ona, wotshita m' munda alindira dzobala dzabwino dzopa-
mbana dza dziko, ali wakulongosoka pa idzo, kwa ntawi
8 dzilandira mvula yapatsogolo ndi mvula yapambuiu. Kalani
olongosoka inu unso; limbikani mitima yanu: kuti kudza
9 kwa Mwini kuli pafupi. Musandandaula, abali, modzi pa
wina, kuti musaweruzidwa; onani, woweruza aima patsogolo
10 pa dzitseko. Tengani, abali, kwa sonyezo la kumva ndi la
kulongosola, aprofeti omwe analankula m' dzina la Mwini.
11 Onani, titsha awo odala omwe anamvabe: munamva ndi
kulongosola kwa Yobi, ndimo munaona kuta kwa Mwini,
bwanje kuti Mwini ali wodzaza ndi tshisoni, ndi wansisi.
12 Koma kopambana zintu zonse, abali anga, musalumbira,
kapena ndi kumwamba, kapena ndi pansi, kapena ndi lumbiro
lina: koma ea wanu akale ea, ndi iai wanu *akale* iai; kuti
musadzagwa pansi pa kuweruza.
13 Kodi alipo modzi mwa inu kumva? apempe. Alipo modzi
14 wosekera? alemekeze. Alipo modzi mwa inu adwala? aitane
akuru a eklesia; ndimo awo apempere pa ie, kudzosa ie ndi
15 mafuta m' dzina la Mwini: ndi pempero la mvanu lidzapulu-
mutsa emwe adwala, ndimo Mwini adzaukitsa ie; ndimo ngati
16 anatshita zimpulupulu, tshidzakulukidwa kwa ie. Ndimo
vumbulutsani mpulupulu zanu modzi ndi wina, ndimo
pemperani modzi kwa wina, monga kuti mungotshiritsidwa.
Pempo la muntu wodeka lilimbika kwambiri m' kutshita
17 kwatshi. Eliya anali muntu wa kufuna kofana ndi ife,
ndimo napempera kolimba kuti kusanangobvumba mvula;
ndimo kusanabvumba mvula pa ntaka kwa dzaka dzitatu
18 ndi miezi isanu ndi umodzi. Ndimo napempera anso; ndimo
kumwamba kunapatsa mvula, ndimo ntaka inabala dzobala
dzatshi.
19 Abali anga, ngati modzi mwa inu asotshera kwa nteradi,
20 ndimo modzi atembenuza ie; adziwe, kuti ie emwe atembe-
nuza wampulupulu kwa tshimo la njira yatshi adzapulumutsa
nzimu kwa imfa, ndimo adzapfunda ambiri a zimpulupulu.

EPISTOLA LATSHIMODZI LA

# PETROS.

PETROS, mpostile wa Yesu Kristu, kwa osang'kidwa 1
omwe ali aulendo a Kubalalika m' Ponto, *m'* Galatiya,
*m'* Kapadokiya, *m'* Asiya, ndimo *m'* Bitiniya, kwa kudziwa- 2
patsogolo kwa Mulungu Atate, m' kuyeretsa kwa Nzimu,
kwa kumvera ndi kuwaza kwa mwazi wa Yesu Kristu:
Kufatsa kwa inu ndi ntendere zipindulidwe.
Wodala *akale* Mulungu ndi Atate a Mwini watu Yesu 3
Kristu, emwe kwa nsisi yatshi yeikuru anabala ife enso kwa
kulingalira kwamoyo ndi kuukirira kwa Yesu Kristu kwa
akufa, kwa zoloa zosabvunda, ndi zosadetsedwa, ndi zomwe 4
zosanyala, zosungidwa m' mwamba kwa inu, omwe ndi 5
mpamvu ya Mulungu adikiridwa mwa mvanu kwa kupulu-
mutsa kuta ku sonyezedwa mwa ntawi yakutungo. Mwa 6
yomwe musekera kwambiri, kapena tsopano kwa ntawi
yeing'ono, ngati kukanali, munapangidwa ku kala ndi
tshisoni mwa mayeso ambiri, monga kuti kuyesera kwa 7
mvanu wanu, *uli* wolemera wopambana golide lomwe
limwazika ngati lingoyeseredwa ndi moto, kunangopezedwe
kwa kulemekeza ndi kupambana ndi ulemu kwa kusonyeza
kwa Yesu Kristu: emwe simunamona mukonda; ndi emwe, 8
ngati tsopano musamona, koma kumvana, musekera kwa-
mbiri ndi tshimwemwe tshosadziwa ku lankulidwa ndi
tshodzaza ndi kupambana: kulandira nsonga ya mvanu 9
wanu, *inde* kupulumutsa kwa mizimu *yanu*. Ndi kupulu- 10
mutsa kumene aprofeti nafuna nasaka kwatshangu, omwe
nalosa ndi kufatsa komwe *kukafika* kwa inu: kusaka *ntawi* 11
iti kapena makalidwe anje a ntawi Nzimu wa Kristu womwe
unali mwa awo unasonya, ntawi unamariza patsogolo zopwe-
tekwa za Kristu, ndi mapambano omwe akatsata izo.
Kwa omwe tshinasonyezedwa, kuti si kwa awo oka, koma 12
kwa inu, anaimirira zintu zimenezi, zomwe tsopano zina-
uzidwa kwa inu mwa iwo omwe anauzidwa ivangeli kwa
inu ndi Nzimu Woyera wotumidwa ku mwamba; zintu
zomwe anjelo afuna ku yang'anira.

13 Mwa tshomwe kumanga mtshunu mwa muwongo wanu,
kalani ape ndimo ikani kota kulingalira kwanu pa kufatsa
komwe kudzatengedwa kwa inu pa kusonyeza kwa Yesu
14 Kristu; monga ana a kumvera, si kufanikiza inu noka
ofana ndi mafuno anu akali mwa *ntawi ya* kupulukira
15 kwanu: koma wofana ndi ie emwe akuitanani ali woyera,
kalani inu noka anso oyera m' makalidwe onse a kukala ndi
16 moyo; tshifuka kuti tshilembedwa, Mudzakala oyera; kuti
17 diri woyera. Ndimo ngati muitana pa ie monga Atate,
emwe wopanda tsang'ko aweruza kofana ndi ntshito ya antu
18 onse, pisani ntawi ya ulendo wanu m' kuopa: kudziwa kuti
munaomboledwa, si ndi zintu zidziwa ku bvunda, ndi
silivere kapena golide, kwa makalidwe atshabe anu a moyo
19 analandiridwa kwa atatu anu; koma ndi mwazi wolemera,
monga wa mwana wa nkosa wopanda kalama ndi wopanda
20 banga, *inde mwazi* wa Kristu: emwe wadziwidwa-patsogolo
nditu patsogolo pa kuzika kwa dziko, koma wasonyezedwa
21 pa nsonga ya zintawi kwa inu, omwe mwa ie ali amvanu ndi
Mulungu, emwe anamukitsa kwa akufa, nampatsa kupa-
mbana; monga kuti mvanu wanu ndi kulingalira zinango-
22 kala m' Mulungu. Kuona munasambitsa mizimu yanu
m' kumvera kwanu kwa nteradi kwa kukonda kosa-
nyenga kwa abali, kwa ntima kondani kolimba modzi ndi
23 wina: kunabadwa anso, si ndi mbeu zobvunda, koma ndi
zosabvunda, mwa mau a Mulungu emwe akala ndi moyo
24 ndimo akalabe. Kuti,

Nyama zonse ziri monga maudzu,
Ndi kupambana konse kwa zimene monga lua la
maudzu.
Maudzu anyala, ndi liu ligwa:
25 Koma kunena kwa Mwini kukala ntawi yonse.

Ndimo kumene kuli kunena kwa makalidwe abwino komwe
kunauzidwa kwa inu.

2 Ndimo kutshotsa mpulupulu zonse, ndi zonama zonse, ndi
2 zinyengo, ndi madano, ndi kulankula konse koipa, monga
makanda abadwa tsopano, funirani nkaka wanzimu womwe
uli wopanda kunama, kuti mungokula ndi umene kwa
3 kupulumutsa; ngati munalawa kuti Mwini ali wokoma
4 ntima: kwa emwe kudza, mwala wamoyo, wataiikidwa
nditu ndi antu, koma ndi Mulungu wosang'kidwa, wolemera,
5 inu unso, monga miala yamoyo, mumangidwa nyumba
yanzimu, ku kala udzukuru woyera, ku tsira nsembe

zanzimu, zolandiridwa ndi Mulungu mwa Yesu Kristu.
Tshifuka asungidwa m' lemba, 6

Ona, diika m' Ziyon mwala *womwe uli* mutu wa
ngondia, wosang'kidwa, wolemera:
Ndi ie emwe amvana ndi ie sadzaikidwa ku manyazi.

Ndimo kwa inu omwe mumvana kuli kulemera: koma 7
kwa omwe osamvana,

Mwala womwe omanga anautaia,
Womwe unapangidwa mutu wa ngondia;

ndimo, 8

Mwala wa kupuntwa, ndi tantwe la tshimo;

kuti apuntwa ndi mau, kuli osamvera: pomwe enso anaiki-
dwa. Koma muli gulu losang'kidwa, udzukuru wofumu, 9
ntundu woyera, antu *ku kala* kupotshera kwa *Mulungu*,
kuti mungosonyeza maubwino opambana a ie emwe anaitana
inu kwa ndima mwa kuunika kwatshi kozizwa: omwe 10
ntawi inapita sinali antu, koma tsopano ali antu a Mulungu:
omwe sanalandira nsisi, koma tsopano analandira nsisi.

Okondedwa, dipempa inu monga aulendo ndi olendo, ku 11
leka mafuno anyama, omwe apanga nkondo pa nzimu; kuli 12
ndi kudzitangata kwanu kwabwino mwa Mitundu; kuti,
mwa tshimene inena pa inu monga otshitazoipa, ndi ntshito
zanu zabwino, zomwe iziona, ingopambanitsa Mulungu m'
siku lakuyang'anira.

Kalani pansi pa miambi yonse ya antu kwa Mwini: 13
kapena kuli ku fumu yotshuka, monga wopambana;
kapena kwa oweruza, monga atumidwa ndi ie kwa 14
kuzimbula pa otshitazoipa ndi kwa kusimba ku omwe
atshita bwino. Kuti tshointshi kuli kufuna kwa Mulungu, 15
kuti ndi kutshitabwino mukatontoletsa kopulukira kwa
antu opusa: monga aufulu, ndi kusatshita ndi ufulu wanu 16
kwa tshopfunda tsha mpulupulu, koma monga akapolo a
Mulungu. Lemekezani antu onse. Kondani ubali. Opani 17
Mulungu. Lemekezani fumu yotshuka.

Abandazi, kalani pansi pa ambuiye anu ndi kuopa konse: 18
si kwa abwino ndi aulere oka, koma anso kwa ankarwe.
Kuti kumene kuli kufatsa, ngati kwa kudzidziwitsa kwa 19
Mulungu muntu amvabe dzisoni, kumva kosadeka. Kuti 20
kupambana kwanje kuli, ngati, ntawi mutshimwa, ndimo
mubwandulidwa *kwa kumene*, mudzamvabe? koma ngati,
ntawi mutshita bwino, ndimo mumva *kwa kumene* mudza-
mvabe, tshimene tshiri kufatsa ndi Mulungu. Kuti kwa 21

kumene munaitanidwa: tshifuka Kristu unso anamva kwa
inu, kusia kwa inu sonyezo, kuti mukatsata miendo yatshi:
22 emwe sanatshita kantu koipa, kapena tshinyengo tshosana-
23 pezedwa m' nkamwa mwatshi: emwe, ntawi anaputwa,
sanaputa anso; ntawi anamva, sanaambirira; koma
24 na*dzi*pereka kwa iemwe aweruza kodeka: emwe ie eka
nanyamula zakwaipa zatu m' tupi latshi pa ntengo, kuti ife,
tinafa kwa zakwaipa, tinangokala ndi moyo kwa kudeka; ndi
25 mikakato ya emwe munatshiritsidwa. Kuti munalikuso-
tshera ofana ndi zinkosa; koma tsopano munabwera kwa
Mbusa ndi Woyang'anira wa mizimu yanu.

3 Tshointsho, akazi inu, kalani pansi pa amuna anu; kuti,
inde ngati ena osamvera mau, opanda mau angolandiridwa
2 ndi makalidwe a akazi ao; kuona makalidwe anu oyera
3 *amangidwa* ndi kuopa. *Kukonza* kwa omwe sikukale
kukonza kunja kwa kuluka tsisi, ndi kwa kubvala zolemera
4 za golide, kapena kubvala nsaru; koma *akale* muntu wobisala
wa ntima, mwa *nsaru* zosadziwa ku bvunda za nzimu woanja
ndi watshete, womwe uli m' kuona kwa Mulungu wa ntengo
5 wapatali. Kuti tshointshi kali akazi oyera anso, omwe
analingalira m' Mulungu, anadzikonza, ali pansi pa amuna
6 ao: monga Sara namvera Abraham, kutsha ie mwini: ana
a emwe muli tsopano, ngati mutshita bwino, ndimo simukala
ndi kuopa ndi kantu koopsa.
7 Amuna inu, tshointsho, kalani ndi *akazi anu* ndi kudziwa,
kupatsa ulemu kwa nkazi, monga kwa tshiwira tshosalimba
tshopambana, monga ali inso oloa anzanu akufatsa kwa moyo;
monga kuti mapempero anu osatshedwetsedwa.
8 Kwakutungo, *kalani* onse inu ndi muwongo umodzi,
9 atshisoni, kukonda monga abali, ogwa ntima, osadzitama: si
kubweza kuipa kwa kuipa, kapena kuputa kwa kuputa;
koma pandunji kudala; kuti kwa tshimene munaitanidwa,
10 monga kuti mukaloa m' dalo. Kuti,

Iemwe afuna ku konda moyo,
Ndi ku ona masiku abwino,
Aletse lilume latshi kwa mpulupulu,
Ndi milomo yatshi kuti yosalankula tshinyengo:
11 Ndimo atembenuke kwa mpulupulu, ndimo atshite bwino;
Afune ntendere, ndi ku saka iwo.
12 Tshifuka kuti maso a Mwini ali pa odeka,
Ndi makutu atshi kwa kupempa kwao:
Koma nkope ya Mwini iri pa awo omwe atshita kuipa.

Ndimo ie ali ndani emwe adzapweteketsa inu, ngati mukala 13
atshitsanzo a tshomwe tshiri tshabwino? Koma ndimo 14
ngati mukamva kwa kudeka, odala *muli inu:* ndimo
musaopa kuopa kwao, kapena musantuntumiridwa; koma 15
yeretsani m' mitima yanu Kristu monga Mwini: *kuli* akuta
ntawi yonse ku yang'ka antu onse omwe afunsa inu tshifukwa
ndi kulingalira komwe kuli mwa inu, koma ndi kuanja ndi
kuopa: kuli ndi kudzidziwitsa kwabwino; kuti, mwa 16
kumene mulankulidwa pa, angoikidwa ndi manyazi omwe
anyansa makalidwe a moyo wanu abwino mwa Kristu.
Kuti kuli kwabwino, ngati kufuna kwa Mulungu kungofuna, 17
kuti mumva kwa kutshitabwino kopambana kwa kutshita
koipa. Tshifuka kuti Kristu unso anamva kwa zoipa ntawi 18
imodzi, wodeka kwa osadeka, kuti anangotenga ife kwa
Mulungu; kunapedwa m' nyama, koma kunasitsimukidwa
m' nzimu; m' womwe enso namuka nauza kwa mizimu m' 19
nyumba ya ndima, yomwe kali inali yosamvera, ntawi kumva 20
kutali kwa Mulungu kunalinda m' masiku a Nowa, ntawi
arke linalikukonzetswa, momwe owereng'jeka, tshomwe
tshiri, mizimu isanu ndi itatu, inapulumutsidwa mwa madzi:
omwe enso m' fanizo loona apulumutsa inu tsopano, *inde* 21
mbapatisma, si kutshotsa kwa litsiro la nyama, koma kufunsa
kwa kudzidziwitsa kwabwino kwa Mulungu, mwa kuukirira
kwa Yesu Kristu; emwe ali pa dzanja lamanja la Mulungu, 22
anaenda mwa mwamba; anjelo ndi oweruza ndi zimpamvu
zinaikidwa pansi pa ie.

Ndimo monga Kristu anamva m' nyama, bvalirani inu 4
noka anso ndi muwongo umodzi; kuti iemwe anamva m'
nyama waleka kwa mpulupulu; kuti ntawi ina simukakala 2
ndi moyo kutsala kwa ntawi zanu m' nyama kwa mafuno a
antu, koma kwa kufuna kwa Mulungu. Kuti ntawi inapita 3
ingotshuruka kunatshita kufuna kwa Mitundu, ndi kunaenda
m' kufuna tshigololo, mafuno oipa, kumwa vinyo, kubvina
kwambiri, kuledzera, ndi kupembedza mafano konyansa:
mwa zimene aganiza kuli kozizwa kuti musatamanga na*o* 4
m' kutshuruka komwe kwa kusaruka, kunena koipa ndi
*inu:* omwe adzawereng'jera kwa iemwe alikuta ku weruza 5
amoyo ndi akufa. Kuti kwa nsonga imene ivangeli unauzi- 6
diwa inde kwa akufa, kuti anangoweruzidwa ofana ndi antu
m' nyama, koma anangokala ndi moyo kwa Mulungu m'
nzimu.

Koma kumariza kwa zintu zonse kuli pafupi: ndimo 7

dziweruzeni, ndimo kalani osaledzera kwa mapempero:
8 opambana zintu zonse kukala atshitutu mwa kukonda kwanu
mwa inu noka; kuti kukonda kubisa zambiri za mpulupulu:
9 kusungira olendo modzi ndi wina kopanda kundandaula:
10 monga onse analandira ntulu, kuimirira ndi iyo mwa inu
noka, monga adindo abwino a kufatsa kwakupindula kwa
11 Mulungu; ngati muntu modzi alankula, *kulankula* monga
anali mau a Mulungu; ngati muntu modzi aimirira,
*kuimirira* monga ndi kulimba komwe Mulungu akwanitsa:
monga kuti m' zintu zonse Mulungu angopambanitsidwa
mwa Yesu Kristu, kwa emwe kuli kupambana ndi umwini
kwa magonero a magonero. Amen.
12 Okondedwa, musaganiza kuli kozizwa ndi muyeso wofana
ndi moto mwa inu, womwe ufika pa inu ku yesa inu, monga
13 ngati kantu kozizwa kanafika kwa inu: koma monga kuti
muli ogawana a kumva kwa Kristu, sekerani; kuti pa
kusonyeza kwa kupambana kwatshi inso mungosekera ndi
14 tshimwemwe tshambiri. Ngati mutonzedwa kwa dzina la
Kristu, odala *muli inu;* tshifuka *Nzimu* wa kupambana
15 ndimo Nzimu wa Mulungu ukala pa inu. Kuti palibe modzi
wa inu amve monga wambanda, kapena woba, kapena
wotshitazoipa, kapena monga wotengera m' ntshito za antu
16 ena: koma ngati *muntu amva* monga Mkristu, ie si akale
ndi manyazi; koma apambanitse Mulungu m' dzina limene.
17 Kuti ntawi *ifika* kwa kuweruza ku amba pa nyumba ya
Mulungu: ndimo ngati *kuamba* patsogolo pa ife, tshiani
*tshidzakala* kumariza kwa omwe osamvera ivangeli wa
18 Mulungu? Ndimo ngati wodeka apulumutsidwa kolimba,
wosadziwa Mulungu ndi wampulupulu zidzasonyeza kuti?
19 Ndimo awo onso omwe amva kofana ndi kufuna kwa
Mulungu aikirire mizimu yao m' kutshita bwino kwa
Wopanga wamvanu.

5 Ndimo akuru mwa inu ditaulira, emwe diri mkuru nzanu,
ndi womariza wa kumva kwa Kristu, emwe diri inso woga-
2 wana wa kupambana komwe kudzasonyezedwa: Busa gulu
la Mulungu lomwe liri mwa inu, kuyang'anira, si kwa
kufulumiza, koma kofuna, kwa Mulungu; kapena kosuntira
si kwa ndrama zonyansa, koma kwa kuta kwa muwongo;
3 kapena si monga kudzikulitsa pa ntshito ipatsidwa kwa inu,
4 koma kupanga inu noka masonyezo ku gulu. Ndimo ntawi
Mbusa wang'kuru adzasonyezedwa, mudzalandira tshisoti
5 tshotshuka tsha kupambana tshomwe tshosanyala. Tsho-

intsho, inu ang'ono, kalani pansi pa akuru. Inde, inu nonse
mangitsani inu noka ndi kusadzitama, ku kala pansi pa
modzi ndi wina: kuti Mulungu akana odzitama, koma apatsa
kufatsa kwa osadzitama. Ndimo dzitshepetseni pansi pa 6
dzanja lampamvu la Mulungu, kuti angokulitsa inu m' ntawi
yabwino; kutaia kuganizaganiza konse kwanu pa ie, tshi- 7
fuka ayang'anira inu. Musaledzera, kalani odikira: liwongo 8
lanu diabolos, monga mkango wopfula, liendaenda, kufuna
emwe lingomwaza: emwe mukana olimba mwa mvanu wanu, 9
kudziwa kuti kumva komwe kulikuta mwa abali anu omwe
ali m' dziko. Ndimo Mulungu wa kufatsa konse, emwe 10
naitana inu kwa kupambana kwatshi kosamariza mwa
Kristu, pambuiu kuti munamva ntawi yeing'ono, ie eka
adzata, adzalimbika, adzalimbitsa inu. Kwa ie *kuli* umwini 11
kwa magonero a magonero. Amen.

Ndi Silvano, mbali wamvanu watu, monga diganiza *ie*, 12
dalemba kwa inu pang'ono, kutaulira, ndi kumariza kuti
kumene kuli kufatsa kwanteradi kwa Mulungu: imani
kolimba mwa kumene. Emwe ali m' Babilon, wosang'kidwa 13
ndi *inu*, autsa inu; ndimo *tshointsho atshita* Marko mwana
wanga. Utsani modzi ndi wina ndi kumsomsona kwa 14
kukonda.

Ntendere kwa inu nonse omwe muli m' Kristu.

---

## EPISTOLA LATSHIWIRI LA

# PETROS.

SIMON PETROS, kapolo ndi mpostile wa Yesu Kristu, 1
kwa omwe analandira mvanu wolemera modzimodzi ndi
ife m' kudeka kwa Mulungu watu ndi Mpulumutsi Yesu
Kristu: Kufatsa kwa inu ndi ntendere zipindulidwe m' 2
kudziwa kwa Mulungu ndi kwa Yesu Mwini watu; kuona 3
kuti mpamvu yamulungu yatshi yapatsa kwa ife zintu zonse
zomwe zikala kwa moyo ndi kupembedza, mwa kudziwa

kwa iemwe anaitana ife ndi kupambana kwatshi ndi ubwino
4 watshi; mwa zimene wapatsa kwa ife malonjezano atshi
olemera ndi akuru nditu; kuti mwa amene mungokala
ogawana a makalidwe amulungu, munapulumuka kwa
5 kubvunda komwe kuli m' dziko ndi kufuna. Inde, ndi
kwa tshifukwa tshimenetshi kuong'khetsa mwa inu tshangu
tshonse, mwa mvanu wanu kwanitsani ubwino; ndimo
6 mwa ubwino *wanu* kudziwa; ndimo mwa kudziwa
*kwanu* kudzikaniza; ndimo mwa kudzikaniza *kwanu* ku-
longosola; ndimo mwa kulongosola *kwanu* kupembedza;
7 ndimo mwa kupembedza *kwanu* kukonda kwa abali; ndimo
8 mwa kukonda *kwanu* kwa abali kukonda. Kuti ngati
zintu zimenezi ziri zanu ndimo zitshuruka, zipanga inu
ku kala si olesi kapena si osabala dzobala kwa kudziwa
9 kwa Mwini watu Yesu Kristu. Kuti iemwe alibe zintu
zimenezi ali wakungu, kuona zomwe zoka ziri pafupi, anai-
10 wala kutsuka kwa zakwaipa zatshi zakali. Mwa tshomwe,
abali, patsani tshangu tshopambana ku limbikitsa kuitana
kwanu ndi kusang'ka kwanu: kuti ngati mutshita zintu
11 zimenezi, musadzapuntwa ntawi ina: kuti tshointsho kudza-
kwanitsidwa kolemera kwa inu kuloa mwa dziko losamariza
la Mwini watu ndi Mpulumutsi Yesu Kristu.
12 Mwa tshomwe didzata ntawi yonse ku kumbutsa inu ndi
zintu zimenezi, ngati muzidziwa, ndi mulimbikitsidwa m'
13 nteradi womwe uli ndi *inu.* Ndimo diganiza tshiri tsha-
bwino, monga kutali monga diri m' msasa umene, ku
14 fulumiza inu ndi kukumbutsa inu; kudziwa kuti kubvula
kwa msasa wanga kudza nsanga, inde monga Mwini watu
15 Yesu Kristu anasonya kwa ine. Inde, didzapatsa tshangu
kuti pa ntawi yonse mudzakala ndi mpamvu pambuiu imfa
16 yanga ku kumbukila zintu zimenezi. Kuti sitinatsata
ntano zopangidwa kotshenjera, ntawi tinadziwitsa inu
mpamvu ndi kudza za Mwini watu Yesu Kristu, koma tinali
17 oonetsa a ukuru watshi. Kuti analandira kwa Mulungu
Atate ulemu ndi kupambana, ntawi linadza kwa ie liu lotere
kwa kupambana kwabwino, Amene ali Mwana wanga
18 wondikonda, mwa iemwe disekera bwino: ndi liu limene
tinamva *ife toka* linaturuka kumwamba, ntawi tinali ndi ie
19 m' piri loyera. Ndimo tiri ndi mau a kulosa *apangidwa*
olimba opambana; kwa amene mutshita bwino kuti
musamala, monga kwa muni kuwala m' malo a ndima,
kwa ntawi siku libanda kutsha, ndimo ntanda iuka m'

mitima yanu: kudziwa tshimene tshoamba, kuti palibe 20
kulosa kwa lemba kuli kwa kusandukidwa koka. Kuti 21
palibe kulosa ntawi yapita kunadza ndi kufuna kwa muntu:
koma antu nalankula kwa Mulungu, kusuntidwa ndi
Nzimu Woyera.

Koma nauka Aprofeti onama anso mwa antu, monga 2
mwa inu unso adzakala apunzitsi onama, omwe adzaloetsa
kutseri zinjiru zomwaza, kukana inde Mpunzitsi emwe
anagula awo, kutenga pa awo oka kumwaza kwansangu.
Ndimo ambiri adzatsata ntshito zao zatshigololo; tshifuka 2
tsha omwe njira ya nteradi idzanenedwa koipa naiyo.
Ndimo m' kusirira ndi mau onyenga adzapanga maronda 3
a inu: kusutsa kwa omwe tsopano kwa kali kusatshedwa,
ndimo kumwaza kwao kusasinza. Kuti ngati Mulungu 4
sanaianja anjelo ntawi anatshimwa, koma naponya awo
pansi kwa Tartaro, naika awo ku maenje a ndima, ku
dikiridwa kwa kuweruza; ndimo sanaianja dziko lakali, 5
koma nasunga Nowa ndi ena asanu ndi awiri, wakuuza wa
kudeka, ntawi natenga tshigumula pa dziko la antu osa-
pembedza; ndimo kutembenuza mizinda ya Sodom ndi 6
Gomora kwa mapulusa nasutsa iyo ndi kugwetsa, kuna-
panga iyo msonyo kwa awo omwe akakala osapembedza:
napulumutsa Lote wodeka, anakala ndi tshisoni tshambiri 7
ndi moyo watshigololo wa oipa (kuti muntu wodeka amene 8
kukala mwa awo, m' kuona ndi m' kumva, nadzisautsa
nzimu *watshi* wodeka kwa siku ndi siku ndi ntshito *zao*
zosamveka): Mwini adziwa bwanje ku pulumutsa apembe- 9
dzi kwa tshinyengo, ndi ku sunga osadeka pa kulanga kwa
dzua la kuweruza; koma kopambana awo omwe aenda 10
pambuiu nyama mwa kufuna kwa kudetsa, ndimo anyoza
umwini. Olimbika, ofuna kwao, osantentemera ku nyoza pa
mapambano: koma anjelo, ngati akuru ndi kulimba ndi 11
mpamvu, osatenga kuweruza konyoza pa awo patsogolo
pa Mwini. Koma amene, monga zamoyo zopanda dingalira, 12
abadwa nyama zoka ku gwidwa ndi ku mwazidwa, kunyoza
ndi zintu ndi zomwe ali opulukira, m' kumwaza kwao
adzamwazidwa nditu, kumva kuipa monga kulipira kwa 13
kutshita kuipa; *antu* omwe aganiza kuli kusekera ku
ledzera m' msana, manga ndi dzilama, kuledzera m' kudia
kwa kukonda ntawi adia ndi inu; kuli maso odzaza ndi 14
tshigololo, ndimo osadziwa ku leka mpulupulu; kunyenjera
mizimu yosalimbika; kuli ndi ntima wakuyesayesa m'

15 kusirira; ana a kutukwana; kusia njira yabwino, naso-
tshera, anatsata njira ya Bileham *mwana* wa Behore, emwe
16 nakonda kulipira kwa kutshita kuipa; koma anasulumu-
lidwa kwa tshimo latshi loka: buru wosalankula, nalankula
17 ndi liu la muntu naletsa misala ya mprofeti. Amene ali
akasope opanda madzi, ndi khungu zikang'kidwa ndi
mondwe; kwa omwe kuda kwa ndima kunasungidwa.
18 Kuti, kulankula *mau* akuru obalawaza a kudzitama, anye-
njera m' mafuno a nyama, ndi kufuna kwa tshigololo, awo
omwe alikupulumuka kolimbika kwa omwe akala m' tshimo;
19 kulonjezana awo ufulu, ntawi awo oka ali akapolo a
kubvunda; kuti wa emwe muntu apambanitswa, wa ie
20 emwe enso atengedwa mwa umpawi. Kuti ngati, pambuiu
anapulumuka zodetsa za dziko mwa kudziwa kwa Mwini ndi
Mpulumutsi Yesu Kristu, atombosola anso mwa izo napa-
mbanitswa, makalidwe akutungo akala nao oipa opambana
21 ndi apatsogolo. Kuti kunali kwabwino kwa awo sikuna-
dziwa njira ya kudeka, kopambana, pambuiu kudziwa iyo,
22 ku bwera kwa mau oyera apatsidwa ku awo. Kunatshiti-
dwa ndi awo ofana ndi ntanti yanteradi, Garu kubwera
anso ku kusanza kwatshi, ndi nkhumba yomwe inasamba
ku kung'khunika m' tope.

3 Limene liri tsopano, okondedwa, epistola latshiwiri lomwe
dilemba kwa inu; ndimo mwa awa awiri difulumiza mu-
2 wongo woona wanu ndi kukumbutsa inu; kuti mukaku-
mbukila mau omwe ananenedwa patsogolo ndi aprofeti
oyera, ndi mau a Mwini ndi Mpulumutsi mwa apostile anu:
3 kudziwa kumene koiamba, kuti m' masiku akutungo anyoza
4 adzafika ndi kunyoza, kuenda pambuiu pa mafuno ao, ndi
kuti, Lonjezano la kufika kwatshi liri kuti? kuti, kwa siku
lomwe atate anagona, zintu zonse zikalabe monga zinali kwa
5 kuamba kwa kupanga. Kuti tshimene aiwala kofuna, kuti
inali miamba kwa pakali, ndi dziko labulungizwa mwa madzi
6 ndi pakati pa madzi, ndi mau a Mulungu; ndi zintu zimene
dziko lomwe linali pa ntawi imene, linagumulidwa ndi
7 madzi, linamwazika: koma miamba yomwe iri tsopano, ndi
dziko, ndi mau amenewa zinaikidwa kwa moto, kusungidwa
pa dzua la kuweruza ndi *la* kumwaza a antu osapembedza.
8 Koma musaiwala tshintu tshimodzi tshimene, okondedwa,
kuti siku limodzi liri ndi Mwini monga dzaka zousan,
9 ndi dzaka zousan monga siku limodzi. Mwini wosatshedwa
ndi lonjezano latshi, monga ena aganiza ndi kutshedwa;

koma amva ntawi yeitali kwa inu, sikufuna kuti modzi
akamwazika, koma kuti onse akafika kwa kutembenuza ntima.
Koma siku la Mwini lidzadza monga woba; momwe miamba 10
idzapita ndi namalowe wang'kuru, ndi zoiamba zidzasungu-
nutsidwa ndi tshitutu tshatshikuru, ndi dziko ndi ntshito
zomwe ziri mwa ilo zidzaotshedwa. Kuona kuti zintu 11
zimene ziri tshointshi zonse ku sungunutsidwa, antu anje
mukanakala m' kukala ndi moyo *konse* koyera ndi kupe-
mbedza, kuyang'anira ndi kufuna kwambiri kudza kwa siku 12
la Mulungu, ndi tshifukwa tsha tshomwe miamba iri kupsa
idzasungunutsidwa, ndi zoiamba zidzasungunuka ndi tshi-
tutu tshatshikuru? Koma, lofana ndi lonjezano latshi, 13
tiyang'anira kwa miamba yatsopano ndi dziko latsopano,
mwa izo kukala kudeka.

Mwa tshomwe, okondedwa, kuona kuti muyang'anira kwa 14
zintu zimenezi, kalani ndi tshangu kuti mungopezedwa
m' ntendere, opanda banga ndi opanda tshulo m' kuona
kwatshi. Ndimo ganizani kuti kumva kutali kwa Mwini 15
watu kuli kupulumutsa; inde monga mbali watu woko-
ndedwa Paulos anso, kofana ndi nzeru zipatsidwa kwa ie,
analemba kwa inu; monga anso m' maepistola *atshi* onse, 16
kulankula mwa awo ndi zintu zimenezi; momwe zirimo
zintu zina zolimbika ku dziwitsidwa, zomwe opulukira ndi
osalimbika apotola, monga *atshita* anso malemba ena, kwa
kumwaza kwao. Ndimo inu, okondedwa, kudziwa patsogolo 17
*zintu zimenezi*, yang'anirani kani, kunyamulidwa ndi tshimo
la oipa, mugwa kwa kulimbika kwanu. Koma kulani m' 18
kufatsa ndi kudziwa kwa Mwini watu ndi Mpulumutsi Yesu
Kristu. Kwa ie *kukale* kupambana inde tsopano ndi kwa
siku la kugonera. Amen.

---

## EPISTOLA LATSHIMODZI LA

# YOHANE.

TSHOMWE tshinali kwa kuamba, tshomwe tinamva, 1
tshomwe tinaona ndi maso atu, tshomwe tinaya-

2 ng'anira, ndi manja atu anagwira, ndi Mau a moyo (ndi moyo
unasonyezedwa, ndimo taona, ndimo timariza, ndimo tiuza kwa
inu moyo, *moyo* wosamariza, womwe unali ndi Atate, ndimo
3 unasonyezedwa kwa ife); tshomwe taona ndi ku mva tiuza
kwa inu unso, kuti inu unso mungokala ndi unzatu ndi ife:
inde, ndi unzatu uli ndi Atate, ndimo ndi Mwana watshi
4 Yesu Kristu: ndi zintu zimenezi tilemba, kuti tshimwemwe
tshatu tshingodzazidwa.
5 Ndimo kumene kuli kufuna komwe tamva kwa ie, ndimo
titshula kwa inu, kuti Mulungu ali kuunika, ndimo mwa ie
6 palibe ndima konse. Ngati tinena kuti tiri ndi unzatshi ndi
ie, ndimo tienda mundima, tinama, ndimo sititshita nteradi:
7 koma ngati tienda m' kuunika, monga ie ali m' kuunika,
tiri ndi unzatu modzi ndi wina, ndi mwazi wa Yesu Mwana
8 watshi utitsuka kwa mpulupulu zonse. Ngati tinena kuti
tiribe mpulupulu, tidzinyenga, ndi nteradi suli mwa ife.
9 Ngati tivumbulutsa mpulupulu zatu, ali wamvanu ndi
wodeka ku kululukira ife mpulupulu zatu, ndi ku tsuka ife
10 kwa kusadeka konse. Ngati tinena kuti sitatshita
mpulupulu, tipanga ie wonama, ndi mau atshi osali
mwa ife.

2 Tiana tanga, zintu zimenezi dilemba kwa inu, kuti
musangotshita mpulupulu. Ndimo ngati muntu modzi
atshimwa, tiri ndi Nkoswe ndi Atate, Yesu Kristu wodeka:
2 ndimo ie ali dipo kwa mpulupulu zatu; ndimo si kwa zatu
3 zoka, koma anso kwa dziko lonse. Ndimo ndi tshimenetshi
4 tidziwa kuti tidziwa ie, ngati tisunga mau atshi. Emwe ati,
dimdziwa, ndimo wosasunga mau atshi, ali wonama, ndi
5 nteradi suli mwa ie: koma emwe asunga mau atshi, mwa ie
nditu kukonda kwa Mulungu kwatedwa. Ndi tshimenetshi
6 tidziwa kuti tiri mwa ie: emwe ati akala mwa ie akanaenda
ie eka anso inde monga ie naenda.
7 Okondedwa, palibe mau atsopano dilemba kwa inu, koma
mau akali omwe munapotshera kwa kwiamba: mau akali
8 ali mau omwe munamva. Anso, mau atsopano dilemba kwa
inu, tshomwe tshiri tshanteradi mwa ie ndi mwa inu;
tshifuka ndima ulikupita, ndi kuunika koona tsopano
9 kuwala. Emwe ati ali m' kuunika, nakwia ndi mbali
10 watshi, ali mundima inde kwa ntawi yatsopano. Emwe
akonda mbali watshi akala m' kuunika, ndimo palibe
11 tshifukwa tsha kukwiitsa mwa ie. Koma emwe akwia ndi
mbali watshi ali mundima, ndimo aenda mundima, ndimo

wosadziwa komwe apita, tshifuka ndima wapanga maso
atshi akungu.

Dilemba kwa inu, tiana *tanga*, tshifuka mpulupulu zanu 12
zikululukidwa kwa inu kwa dzina latshi. Dilemba kwa inu, 13
atate, tshifuka mudziwa ie emwe ali kwa kwiamba.
Dilemba kwa inu, anyamata, tshifuka munapambana
wampulupulu. Dinalemba kwa inu, tiana, tshifuka mudziwa
Atate. Dinalemba kwa inu, atate, tshifuka mudziwa ie emwe 14
ali kwa kwiamba. Dinalemba kwa inu, anyamata, tshifuka
muli olimba, ndi mau a Mulungu akala mwa inu, ndimo
munapambana wampulupulu. Musakonda dziko, kapena 15
zintu zomwe ziri m' dziko. Ngati muntu modzi akonda
dziko, kukonda kwa Atate sikuli mwa ie. Kuti zonse 16
zomwe ziri m' dziko, kufuna kwa nyama, ndi kufuna kwa
maso, ndi kudzitama kwa moyo, siziri kwa Atate, koma ziri
kwa dziko. Ndimo dziko lipita, ndi kufuna kwa ilo: koma 17
emwe atshita kufuna kwa Mulungu akala kwa ntawi
yosamariza.

Tiana, liri ora lakutungo: ndimo monga munamva kuti 18
wapakristu adza, inde tsopano anauka apakristu ambiri;
ndi komwe tidziwa kuti liri ora lakutungo. Naturuka kwa 19
ife, koma sanali a ife; kuti ngati anali a ife, akanakalabe
ndi ife: koma *naturuka*, kuti anangosonyezedwa bwanje kuti
siali onse a ife. Ndimo mupotshera kudzosa kwa Woyera, 20
ndimo mudziwa zintu zonse. Sindinalemba kwa inu tshi- 21
fuka musadziwa nteradi, koma tshifuka muudziwa, ndimo
tshifuka palibe bodza liri kwa nteradi. Ndani ali wonama 22
koma emwe akana kuti Yesu ali Kristu? Amene ali wapa-
kristu, *inde* emwe akana Atate ndi Mwana. Emwe akana 23
Mwana, ie emwe sali ndi Atate: emwe abvomera Mwana ali
ndi Atate enso. Nanga inu, tshimene tshikale mwa inu 24
tshomwe munamva kwa kwiamba. Ngati tshimene tshomwe
munamva kwa kwiamba tshikala mwa inu, inu unso mudza-
kala m' Mwana, ndimo mwa Atate. Ndimo limene liri 25
lonjezano lomwe analonjezana ndi ife, *inde* moyo wosamariza.
Zintu zimenezi dinalemba kwa inu ndi awo omwe afuna ku 26
sotshereza inu. Ndimo nanga inu, kudzosa komwe munala- 27
ndira kwa ie kukala mwa inu, ndimo musafuna kuti modzi
apunzitsa inu; koma monga kudzosa kwatshi kupunzitsa
inu ndi zintu zonse, ndimo kuli kwanteradi, ndimo kuli
kulibe bodza, ndimo inde monga kunapunzitsa inu, mukala
mwa ie. Ndimo tsopano, tiana *tanga*, kalani mwa ie; kuti, 28

ngati adzasonyezedwa, tingokala ndi kulimbika, ndimo
sitingokala ndi manyazi patsogolo pa ie pa kufika kwatshi.
29 Ngati mudziwa kuti ie ali wodeka, mudziwa kuti onse enso
omwe atshita kudeka abadwa ndi ie.
3 Ona kukonda kwanje Atate wapatsa pa ife, kuti tika-
tshedwa ana a Mulungu : ndimo *otere* tiri. Kwa tshifukwa
tshimene dziko losadziwa ife, tshifuka losanadziwa ie.
2 Okondedwa, tsopano tiri ana a Mulungu, ndimo sitshisonye-
zedwa kosuntira tshomwe tidzakala. Tidziwa kuti, ngati
adzasonyezedwa, tidzakala ofana ndi ie; kuti tidzaona ie
3 inde monga ali. Ndimo onse omwe ali ndi lingaliro limene
4 *liikidwa* pa ie adziyeretsa, inde monga ie ali woyera. Onse
omwe atshita mpulupulu atshita anso kusamveka: ndi
5 mpulupulu iri kusamveka. Ndimo mudziwa kuti anasonye-
zedwa ku tshotsa zimpulupulu; ndimo mwa ie mulibe
6 mpulupulu. Emwe akala mwa ie wosatshita mpulupulu:
emwe atshita mpulupulu sanaona ie, kapena wosadziwa ie.
7 Tiana *tanga*, palibe muntu asotshereze inu: ie emwe atshita
8 kudeka ali wodeka, inde monga ie ali wodeka: ie emwe
atshita mpulupulu ali wa diabolos; kuti diabolos atshimwa
kwa kwiamba. Kwa nsonga imene Mwana wa Mulungu
anasonyezedwa, kuti anangomwaza ntshito za diabolos.
9 Emwe abadwa ndi Mulungu wosatshita mpulupulu, tshifuka
mbeu yatshi ikala mwa ie: ndimo wosadziwa ku tshita
10 mpulupulu, tshifuka abadwa ndi Mulungu. M' tshimene
ana a Mulungu asonyezedwa, ndi ana a diabolos: emwe
wosatshita kudeka si ali ndi Mulungu, kapena ie emwe
11 wosakonda mbali watshi. Kuti amene ali mau omwe
12 munamva kwa kwiamba, kuti tikanakondana: si monga
Kayin anali wa wampulupulu, napa mpwatshi. Ndimo napa
ie kwa tshiani? Tshifuka ntshito zatshi zinali zoipa, ndi za
mpwatshi *zinali* zodeka.
13,14 Musazizwa, abali, ngati dziko likwiira inu. Tidziwa kuti
tapita kwa imfa m' moyo, tshifuka tikonda abali. Emwe
15 wosakonda akala m' imfa. Emwe akwia ndi mbali watshi
ali wambanda: ndimo mudziwa kuti palibe mbanda ali ndi
16 moyo wosamariza kukala mwa ie. M' tshimene tidziwa
kukonda, tshifuka naika pansi moyo watshi kwa ife: ndimo
17 tikanaika pansi mioyo yatu kwa abali. Koma emwe ali ndi
zintu za dziko, ndimo aona mbali watshi m' kusauka, natseka
nsoni yatshi kwa ie, bwanje kukonda kwa Mulungu kukala
18 mwa ie? Tiana *tanga*, tisakonde m' mau, kapena ndi

lilume; koma m' ntshito ndi nteradi. M' tshimene tidza- 19
dziwa kuti tiri kwa nteradi, ndimo tidzalimbikitsa mitima
yatu patsogolo pa ie, m' tshimene mitima yatu isutsa ife; 20
tshifuka Mulungu ali wang'kuru wopambana mitima yatu,
ndimo adziwa zintu zonse. Okondedwa, ngati mitima yatu 21
yosasutsa ife, tiri ndi kulimbika kwa Mulungu; ndimo 22
tshomwe tifunsa, tilandira kwa ie, tshifuka tisunga mau
atshi, ndimo titshita zintu zomwe ziri zosekeretsa m' kuona
kwatshi. Ndi amene ali mau atshi, monga kuti tikanamvana 23
m' dzina la Mwana watshi Yesu Kristu, ndi ku kondana,
inde monga napatsa ife mau. Ndimo emwe asunga mau 24
atshi akala mwa ie, ndi ie mwa ie. Ndimo m' tshimene
tidziwa kuti akala mwa ife, ndi Nzimu womwe anapatsa ife.

Okondedwa, musamvana ndi mizimu yonse, koma yesani 4
mizimu, ngati iri ya Mulungu: tshifuka aprofeti ambiri
onama anaturuka m' dziko. M' tshimene mudziwa Nzimu 2
wa Mulungu: mizimu yonse yomwe ibvomera kuti Yesu
Kristu anafika m' nyama iri ya Mulungu: ndimo mizimu 3
yonse yomwe yosabvomera Yesu siiri ya Mulungu: ndimo
umene uli *nzimu* wa wapakristu, ndi womwe munamva kuti
ufika; ndi tsopano uli m' dziko kali. Muli kwa Mulungu, 4
tiana *tanga*, ndimo munapambanitsa iwo: tshifuka wang'kuru
ali ie emwe ali mwa inu ndi emwe ali m' dziko. Iri kwa 5
dziko: ndimo ilankula *monga* kwa dziko, ndi dziko limva
iwo. Tiri kwa Mulungu: emwe adziwa Mulungu amva 6
ife; emwe wosali kwa Mulungu wosamva ife. Ndi tshi-
mene tidziwa nzimu wa nteradi, ndi nzimu wa tshimo.

Okondedwa, tikondane: kuti kukonda kuli kwa Mu- 7
lungu; ndimo onse omwe akonda abadwa ndi Mulungu,
ndimo adziwa Mulungu. Emwe wosakonda wosadziwa 8
Mulungu; kuti Mulungu ali kukonda. M' tshimene ku- 9
konda kwa Mulungu kunasonyezedwa mwa ife, kuti
Mulungu watumiza Mwana watshi wobadwa eka m' dziko,
kuti tinangokala ndi moyo mwa ie. M' tshimene kuli 10
kukonda, si kuti tinakonda Mulungu, koma kuti anakonda
ife, ndimo natumiza Mwana watshi *ku kala* dipo kwa mpulu-
pulu zatu. Okondedwa, ngati Mulungu tshointsho ana- 11
konda ife, tikanakondana anso. Palibe muntu waona 12
Mulungu pa ntawi ina: ngati tikondana, Mulungu akala
mwa ife, ndimo kukonda kwatshi kutedwa mwa ife:
m' tshimene tidziwa kuti tikala mwa ie, ndi ie mwa 13
ife, tshifuka ie wapatsa ife kwa Nzimu watshi. Ndimo 14

taona ndimo timariza kuti Atate anatumiza Mwana *ku kala*
15 Mpulumutsi wa dziko. Emwe adzabvomera kuti Yesu ali
Mwana wa Mulungu, Mulungu akala mwa ie, ndi ie mwa
16 Mulungu. Ndimo tidziwa ndimo tamvana ndi kukonda
komwe Mulungu apotshera mwa ife. Mulungu ali ku-
konda; ndi emwe akala m' kukonda akala mwa Mulungu,
17 ndi Mulungu akala mwa ie. M' tshimene kukonda ku-
tedwa ndi ife, kuti tingopotshera kulimbika m' dzua la
kuweruza; tshifuka monga ie ali, inde tshointsho tiri
18 m' dziko limene. Mulibe kuopa m' kukonda: koma ku-
konda kwakuta kuturutsa kuopa, tshifuka kuopa kukala ndi
19 kulanga; ndi iemwe aopa sikutedwa m' kukonda. Tikonda,
20 tshifuka ie nakonda ife koiamba. Ngati muntu ati, Diko-
nda Mulungu, ndimo akwia ndi mbali watshi, ie ali wonama:
kuti emwe wosakonda mbali watshi emwe waona, wosadziwa
21 ku konda Mulungu emwe sanaona. Ndi mau amene tipo-
tshera kwa ie, kuti emwe akonda Mulungu akonda mbali
watshi inso.

5 Emwe amvana kuti Yesu ali Kristu abadwa ndi Mu-
lungu: ndi emwe akonda ie emwe anabala akonda ie enso
2 emwe abadwa ndi ie. M' tshimene tidziwa kuti tikonda
ana a Mulungu, ntawi tikonda Mulungu, ndimo titshita mau
3 atshi. Kuti kumene kuli kukonda kwa Mulungu, kuti
4 tisunga mau atshi: ndimo mau atshi osali olemera. Kuti
tshomwe tshibadwa ndi Mulungu tshipambana dziko:
ndimo kumene kuli kupambana komwe kunapambana dziko,
5 *inde* mvanu watu. Ndimo ndani ali emwe apambanitsa
dziko, koma emwe amvana kuti Yesu ali Mwana wa
6 Mulungu? Amene ali emwe anafika ndi madzi ndi mwazi,
*inde* Yesu Kristu; si ndi madzi oka, koma ndi madzi ndimo
7 ndi mwazi. Ndimo uli Nzimu womwe umariza, tshifuka Nzi-
8 mu uli nteradi. Kuti ziripo zitatu zomwe zimariza, Nzimu,
ndi madzi, ndi mwazi: ndimo zitatu zianjana m' modzi.
9 Ngati tilandira kumariza kwa antu, kumariza kwa Mulungu
kuli kwakukuru: kuti kumariza kwa Mulungu kuli kumene,
10 kuti wamariza ndi Mwana watshi. Emwe amvana ndi
Mwana wa Mulungu ali ndi kumariza mwa ie: emwe
wosamvana ndi Mulungu wapanga ie wonama; tshifuka
sanamvana ndi kumariza komwe Mulungu wamariza ndi
11 Mwana watshi. Ndimo kumariza kuli kumene, kuti Mu-
lungu anapatsa kwa ife moyo wosamariza, ndimo moyo
12 umene uli m' Mwana watshi. Emwe ali ndi Mwana ali ndi

moyo; emwe wosali ndi Mwana wa Mulungu wosali ndi
moyo.
Zintu zimenezi dinalemba kwa inu, kuti mungodziwa 13
kuti muli ndi moyo wosamariza, *inde* kwa inu omwe amvana
pa dzina la Mwana wa Mulungu. Ndimo kumene kuli 14
kulimbika komwe tipotshera kwa ie, kuti, ngati tifunsa
kantu ndi kufuna kwatshi, amva ife: ndimo ngati tidziwa 15
kuti amva ife tshomwe tifunsa, tidziwa kuti tipotshera
mafunso omwe tinafunsa kwa ie. Ngati muntu modzi aona 16
mbali watshi kutshita mpulupulu si kwa imfa, adzafunsa,
ndimo *Mulungu* adzampatsa moyo kwa awo omwe osatshita
mpulupulu kwa imfa. Iripo mpulupulu kwa imfa: si ndi
imene dinena kuti akafunsa. Kusadeka konse kuli mpulu- 17
pulu: ndimo iripo mpulupulu si kwa imfa.
Tidziwa kuti emwe abadwa ndi Mulungu wosatshimwa; 18
koma emwe anabadwa ndi Mulungu adzisunga, ndimo
wampulupulu wosatosa ie. Tidziwa kuti tiri kwa Mulungu, 19
ndimo dziko lonse likala m' wampulupulu. Ndimo tidziwa 20
kuti Mwana wa Mulungu anafika, ndimo wapatsa ife kudzi-
wa, kuti tidziwa ie emwe ali woona, ndimo tiri mwa ie
emwe ali woona, *inde* m' Mwana watshi Yesu Kristu.
Amene ali Mulungu woona, ndi moyo wosamariza. Tiana 21
*tanga*, sungani inu noka kwa mafano.

---

### EPISTOLA LATSHIWIRI LA

# YOHANE.

MKURU ku fumu-yeikazi yosang'ka ndi ana atshi, omwe 1
dikonda m' nteradi; ndimo si ine ndeka, koma anso
onse omwe adziwa nteradi; kwa nteradi womwe ukala mwa 2
ife, ndimo udzakala ndi ife kwa ntawi yosamariza: Kufatsa, 3
nsisi, ntendere zidzakala ndi ife, kwa Mulungu Atate, ndi
kwa Yesu Kristu, Mwana wa Atate, m' nteradi ndi kukonda.
Disekera kwambiri kuti dinapeza *ena* a ana ako kuenda 4

5 m' nteradi, inde monga tinalandira mau kwa Atate. Ndimo
tsopano dipempa iwe, fumu-yeikazi, si monga ngati dinalemba
kwa iwe mau atsopano, koma amene omwe tinapotshera
6 kwa kwiamba, kuti tikondana. Ndimo kumene kuli
kukonda, kuti tikaenda pambuiu mau atshi. Amene ali
mau, inde monga munamva kwa kwiamba, kuti mukaenda
7 mwa iwo. Kuti onyenga ambiri anaturuka m' dziko, *inde*
awo omwe osabvomera kuti Yesu Kristu afika m' nyama.
8 Amene ali wonyenga ndi wapakristu. Yang'anirani inu
noka, kuti musamwaza zintu zomwe tinazitshita, koma kuti
9 mulandira kulipira kodzaza. Emwe atsogolera ndimo
wosakala m' kupunzitsa kwa Kristu, wosali ndi Mulungu:
emwe akala m' kupunzitsa, ie ali ndi Atate ndi Mwana.
10 Ngati modzi afika kwa inu, ndimo wosatenga kupunzitsa
kumene, musalandira ie m' nyumba *yanu*, ndimo musamutsa:
11 kuti emwe amutsa agawa ntshito zatshi zoipa.
12 Kupotshera zintu zambiri kulemba kwa inu, sindifuna
*kuzilemba* ndi karata ndi inke: koma dilingalira ku fika kwa
inu, ndimo ku lankula nkope ndi nkope, kuti tshimwemwe
13 tshanu tshingodzazidwa. Ana a mpwako wosang'ka autsa
iwe.

---

EPISTOLA LATSHITATU LA

# YOHANE.

1 MKURU ku Gayo wokondedwa, emwe dikonda m'
nteradi.
2 Wokondedwa, dipempera kuti m' zintu zonse ungolemerera
3 nungokala bwino, inde monga nzimu wako ulemerera. Kuti
dinasekera kwambiri, ntawi abali anafika namariza kwa
4 nteradi wako, inde monga uenda m' nteradi. Tshimwemwe
tshatshikuru diribe tshopambana ndi tshimene, kumva ndi
ana anga kuenda m' nteradi.
5 Wokondedwa, utshita ntshito yamvanu m' tshomwe utshita
6 kwa awo omwe ali abali ndi alendo nditu; omwe anamariza

ndi kukonda kwako patsogolo pa eklesia: omwe udzatshita
bwino ku perekeza pa ulendo wao koenera kwa Mulungu:
tshifuka kuti kwa Dzina anaturuka, kutenga tshabe kwa 7
Mitundu. Ndimo tikanaloetsa otere, kuti tingokala antshito 8
anzao ndi nteradi.

Dinalemba kantu kwa eklesia: koma Diyotrefes, emwe ako- 9
ndaku potshera kupambana mwa awo, wosalandira ife. Ndimo, 10
ngati didza, didzakumbutsa ntshito zatshi zomwe azitshita,
kunena pa ife ndi mau oipa: ndimo anyanyala ndi amene,
kapena wosalandira ie eka abali, ndi awo omwe afuna,
aletsa, naturutsa *awo* mwa eklesia. Wokondedwa, usatsanza 11
tshomwe tshiri tshoipa, koma tshomwe tshiri tshabwino.
Emwe atshita bwino ali kwa Mulungu: emwe atshita kuipa
wosaona Mulungu. Demetriyo ali ndi kumariza kwa *antu* 12
onse, ndi kwa nteradi woka: inde, enso timariza; ndimo
udziwa kuti kumariza kwatu kuli kwanteradi.

Dinali ndi zintu zambiri ku lemba kwa iwe, koma sindi- 13
funa ku*zi*lemba kwa iwe, ndi inke ndi peni: koma dilingalira 14
nsanga ku ona iwe, ndimo tidzalankula nkope ndi nkope.
Ntendere *ukale* kwa iwe. Abali autsa iwe. Utsa abali ndi
maina.

---

EPISTOLA LA

# YUDA.

YUDA, kapolo wa Yesu Kristu, ndi mbali wa Yakobi, ku 1
omwe aitanidwa, okondedwa m' Mulungu Atate, ndi
osungidwa kwa Yesu Kristu: Nsisi kwa inu ndi ntendere 2
ndi kukonda zipindulidwa.

Okondedwa, ntawi dinalikupatsa tshangu tshonse ku 3
lembera inu ndi kupulumutsa kwa onse kwatu, dina-
fulumizidwa ku lembera inu kutaulira inu ku kanganitsana
kwambiri kwa mvanu womwe ntawi imodzi kwa zonse
unaperekedwa kwa oyera. Kuti kunali antu ena analo- 4
ezedwa kutseri, *inde* omwe kali anapakulidwa kwa kusutsa
kumene, osapembedza, kutembenuza kufatsa kwa Mulungu
watu kwa kufuna kwa tshigololo, ndi kukana Mbuiye watu
eka ndi Mwini, Yesu Kristu.

5 Ndimo difuna ku kumbutsa inu, ngati mudziwa zintu
zonse ntawi imodzi kwa zonse, bwanje kuti Mwini, anapulu-
mutsa antu kwa dziko la Yiputa, pambuiu anamwaza awo
6 omwe sanamvana. Ndimo anjelo omwe sanasunga dziko
lao, koma nasia malo ao, anagwira m' zomangira zosamariza
7 pansi pa ndima kwa kuweruza kwa siku lalikuru. Inde
monga Sodom ndi Gomora, ndi mizinda yozungulira iyo,
yofana ndi iyo inapatsidwa iyo yoka kwa dama, ndimo
inatsata nyama zina, isonyezedwa monga sonyezo, kumva
8 kulanga kwa moto wosamariza. Kosuntira tshointsho
amene enso m' kulota kwao adetsa nyama, nabvuta
9 umwini, natukwana opambana. Koma Mikayeli njelo
wopambana, ntawi nakangana ndi diabolos nafukana tupi
la Moses, sanayesa ku tengera pa ie kuweruza kotukwana,
10 koma nati, Mwini asulumula iwe. Koma amene atukwana
ndi zintu zomwe osadziwa: ndi zomwe adziwa ndi makalidwe
ao, ofana ndi zamoyo zopanda dingalira, m' zintu zimenezi
11 amwazidwa. Tshaipa kwa awo! kuti napita m' njira
ya Kayin, nataiika iwo oka m' tshimo la Bileham kwa
12 kulipira, namwazika munseke wa Kora. Amene ali awo
omwe ali matantwe obisidwa mwa kudia kwa kukonda
kwanu ntawi adia ndi inu, abusa omwe opanda manta
adzibusa; mitambo yopanda madzi, itengedwa ndi zimpepo;
mitengo ya masika yopanda dzobala, yafa kawiri, yazulidwa
13 ndi mitsitsi; mafundi olimba a nyanja, kuturuka pobvu la
manyazi ao, nyenyezi zosotshera, kwa zomwe kuda kwa
14 ndima kwasungidwa kwa ntawi yonse. Ndimo kwa amene
enso Henoki, watshisanu ndi tshiwiri kwa Adam, nalosa,
kuti, Ona, Mwini nafika ndi mazousan makumi a oyera
15 atshi, ku tshita kuweruza pa onse, ndi ku tshimika osape-
mbedza onse ndi ntshito zao zonse za kusapembedza zomwe
anazitshita kosapempedza, ndimo ndi zintu zonse zolimba
16 zomwe ampulupulu osapembedza analankula pa ie. Amene
ali ondandaula, akuneneza, kupita kofana ndi mafuno oipa
ao (ndi nkamwa mwao mulankula *mau* akuru obalawaza),
kusonya tsang'ko kwa kupindula.
17 Koma inu, okondedwa, kumbukilani mau omwe ananene-
dwa patsogolo ndi apostile a Mwini watu Yesu Kristu;
18 bwanje kuti nanena ndi inu, Mwa ntawi yakutungo kudza-
kala onyoza, kupita kofana ndi mafuno ao a kusapembedza.
19 Amene ali awo omwe apanga malekanitso, oyaluka, siali
20 ndi Nzimu. Koma inu, okondedwa, mumanga inu noka pa

mvanu wanu woyera wopambana, kupempera mwa Nzimu
Woyera, sungani inu noka m' kukonda kwa Mulungu, 21
kuyang'anira nsisi ya Mwini watu Yesu Kristu kwa moyo
wosamariza. Ndi pa ena kalani ndi nsisi, omwe ali mwa 22
kuganizaganiza; ndi ena pulumutsani, kusompola awo kwa 23
moto; ndi pa ena kalani ndi nsisi ndi kuopa; kukwia inde
mwinjiro wadontotshezedwa ndi nyama.

Ndimo kwa iemwe ali ndi mpamvu ku sunga inu kwa 24
kupuntwa, ndi ku ika inu patsogolo pa nkope ya kupambana
kwatshi opanda kalama mwa tshimwemwe tshatshikuru, kwa 25
Mulungu eka Mpulumutsi watu, mwa Yesu Kristu Mwini
watu, *zikale* kupambana, ukuru, kuweruza ndi mpamvu,
patsogolo pa ntawi yonse, ndimo tsopano, ndi kwa magonero
onse. Amen.

---

KUSONYEZA KWA

# YOHANE.

KUSONYEZA kwa Yesu Kristu, komwe Mulungu na- 1
patsa ie ku sonyeza kwa akapolo atshi, *inde* zintu
zomwe zikanakala nsanga: ndimo natumiza nasonyeza *iko*
ndi njelo watshi kwa kapolo watshi Yohane; emwe ana- 2
mariza ndi mau a Mulungu, ndimo ndi kumariza kwa Yesu
Kristu, *inde* ndi zintu zonse zomwe naziona. Wodala ali ie 3
emwe awerenga, ndi awo omwe amva mau a kulosa, ndimo
asungira zintu zomwe zilembedwa momo: kuti ntawi iri
pafupi.

YOHANE ku maeklesia asanu ndi awiri omwe ali m' Asiya: 4
Kufatsa kwa inu ndi ntendere, kwa ie emwe ali ndi emwe
anali ndi emwe adza; ndi kwa Mizimu isanu ndi iwiri
yomwe iri patsogolo mpando wotshuka watshi; ndi kwa 5
Yesu Kristu, *emwe ali* womariza wamvanu, wobadwa
woiamba kwa akufa, ndi woweruza wa mafumu a dziko.
Kwa emwe atikonda, ndimo anamasula ife kwa mpulupulu
zatu ndi mwazi watshi; ndimo napanga ife *ku kala* dziko, 6
*ku kala* adzukuru kwa Mulungu ndi Atatu atshi; kwa ie
*zikale* kupambana ndi kuweruza kwa magonero a magonero.

7 Amen. Ona, adza ndi mitambo; ndi maso onse adzamona,
ndimo awo omwe anambola; ndi mitundu yonse ya pansi
idzalira pa ie. Inde tshointsho, Amen.
8 Diri Alefa ndi Omega, ati Mwini Mulungu, emwe ali ndi
emwe anali ndi emwe adza, Wampamvuyonse.
9 Ine Yohane, mbali wanu ndi wogawa ndi inu m' sautso
ndi m' dziko ndi m' kulongosola *zomwe ziri* m' Yesu, dinali
m' tshisi tshomwe tshitshedwa Patmo, kwa mau a Mulungu
10 ndi kumariza kwa Yesu. Dinali mwa Nzimu pa dzua la
Mwini, ndimo dinamva pambuiu pa ine liu lalikuru, monga
11 la lipenga linena, Tshomwe uona, lemba m' buku, nutumiza
*ilo* kwa maeklesia asanu ndi awiri; kwa Feso, ndi kwa
Smirna, ndi kwa Pergamo, ndi kwa Tiyatira, ndi kwa Sardis,
12 ndi kwa Filadelfiya, ndi kwa Lawodikeya. Ndimo dina-
tembenuka ku ona liu lomwe linalankula ndi ine. Ndimo
kunatembenuka dinaona zogwirira nyali zisanu ndi ziwiri za-
13 golide; ndi pakati pa zogwirira nyali modzi wofana ndi
mwana wa muntu, wabvekwa ndi mwinjiro pansi pa pazi,
14 namanga pa mabere ndi lamba lagolide. Ndimo mutu
watshi ndi tsisi latshi zinali zoyera monga wulu woyera,
*zoyera* monga nkhungu; ndi maso atshi anali monga lilume
15 la moto; ndi mapazi atshi ofana nkua wong'azimira, monga
ngati unayepulidwa m' ng'anjo; ndi liu latshi monga liu la
16 madzi ambiri. Ndimo anapotshera m' dzanja latshi lamanja
nyenyezi zisanu ndi ziwiri: ndi kwa nkamwa mwatshi
unaturuka mpeni wa nkondo wakutwa konsekonse: ndi
nkope yatshi inali monga dzua liwala m' mpamvu yatshi.
17 Ndimo ntawi dinamona, dinagwa pa mapazi atshi monga
modzi wakufa. Ndimo naika dzanja latshi lamanja pa ine,
18 kuti, Usaopa; Diri woiamba ndi wakutungo, ndi Wamoyo;
ndimo dinafa, ndimo ona, diri ndi moyo kwa magonero a
magonero, ndimo dipotshera zofungulira za imfa ndi za
19 Hadesi. Ndimo lemba zintu zomwe unaziona, ndi zintu
20 zomwe ziri, ndi zintu zomwe zidzakala pambuiu; kusadzi-
wika kwa nyenyezi zisanu ndi ziwiri zomwe unaona m'
dzanja langa lamanja, ndi zogwirira nyali zisanu ndi ziwiri
zagolide. Nyenyezi zisanu ndi ziwiri ziri anjelo a maeklesia
asanu ndi awiri: ndi zogwirira nyali ziri maeklesia asanu
ndi awiri.

2 Kwa njelo wa eklesia m' Feso lemba;
Zintu zimenezi anena ie emwe agwira nyenyezi zisanu ndi
ziwiri m' dzanja latshi lamanja, iemwe aenda pakati pa

zogwirira nyali zisanu ndi ziwiri zagolide: didziwa ntshito 2
zako, ndi kutshita kwambiri kwako ndi kulongosola, ndi
kuti usadziwa ku mva antu oipa, ndi unayesa awo omwe
adzitsha apostile, ndimo osali, ndimo unapeza awo onyenga;
ndimo uli ndi kulongosola ndimo unamva kwa dzina langa, 3
ndimo sunalema. Koma diri ndi *tshimene* pa iwe, kuti unasia 4
kukonda kwako kuamba. Ndimo kumbukila kwa kuti 5
wagwa, ndimo tembenuza ntima, ndi tshita ntshito
zoiamba; kapena kani difika kwa iwe, ndimo didzatshotsa
tshogwirira nyali tshako kwa malo atshi, ngati usatembenuza
ntima. Koma tshimene uli natsho, kuti ukwia ndi 6
ntshito za Nikolawo, zomwe enso dikwiira. Emwe ali kutu, 7
amve tshomwe Nzimu unena ndi maeklesia. Kwa ie emwe
apambana, kwa ie didzapatsa ku dia kwa ntengo wa moyo,
womwe uli m' Paradisi la Mulungu.

Ndimo ku njelo wa eklesia m' Smirna lemba; 8

Zintu zimenezi ati woiamba ndi wakutungo, emwe anafa,
nakala ndi moyo *onso:* Didziwa sautso yako, ndi kusauka 9
kwako (koma uli wolemera), ndi kutukwana kwa awo omwe
anena ali Ayuda, ndimo osali, koma ali Sinagoge la Satana.
Usaopa zintu zomwe utofuna ku mva: ona, diabolos atofuna 10
ku ponya ena a inu m' nyumba ya ndima, kuti mungoye-
sedwa; ndimo mudzapotshera sautso masiku kumi. Kala
wamvanu kwa imfa, ndimo didzapatsa iwe tshisoti tshotshuka
tsha moyo. Emwe ali kutu, amve tshomwe Nzimu unena 11
ndi maeklesia. Emwe apambana sadzapwetekedwa ndi imfa
yatshiwiri.

Ndimo ku njelo wa eklesia m' Pergamo lemba; 12

Zintu zimenezi ati emwe ali ndi mpeni wa nkondo wa-
kutwa konsekonse: Didziwa komwe ukala, *inde* pomwe 13
mpando wotshuka wa Satana uli: ndimo ugwira kolimba
dzina langa, ndimo usanakana mvanu wanga, inde m' masiku
a Antipas womariza wanga, wamvanu wanga, emwe anape-
dwa mwa inu, pomwe Satana akala. Koma diri ndi zintu 14
zowereng'jeka pa iwe, tshifuka pomwe uli ndi ena omwe
asunga kupunzitsa kwa Bileham, emwe napunzitsa Balaki
ku ponya kukwiitsa patsogolo pa ana a Sirayeli, ku dia zintu
zotsiridwa kwa mafano, ndi ku tshita dama. Tshointshi 15
inso uli ndi ena omwe asunga kupunzitsa kwa Nikolawo
modzimodzi. Ndimo tembenuza ntima; kapena kani difika 16
kwa iwe nsanga, ndimo didzapanga nkondo pa awo ndi
mpeni wa nkondo wa nkamwa mwanga. Emwe ali kutu, 17

amve tshomwe Nzimu unena ndi maeklesia. Kwa emwe
apambana, kwa ie didzapatsa wa mana yobisidwa, ndimo
didzampatsa mwala woyera, ndi pa mwala dzina latsopano
linalembedwa, lomwe palibe modzi adziwa koma emwe
alandira ilo.
18 Ndimo kwa njelo wa eklesia m' Tiyatira lemba;
Zintu zimenezi anena Mwana wa Mulungu, emwe ali
ndi maso atshi ofana ndi lilume la moto, ndi mapazi atshi ali
19 ofana ndi nkua yong'azimira: Didziwa ntshito zako, ndi
kukonda kwako ndi mvanu ndi kuimirira ndi kulongosola,
ndi kuti ntshito zako zakutungo ziri zopambana zoiamba.
20 Koma dipotshera *tshimene* pa iwe, kuti ulola nkazi Yezebeli,
emwe adzitsha mprofeti wankazi; ndimo apunzitsa
nasotsheretsa akapolo anga ku tshita dama, ndi ku dia zintu
21 zotsiridwa kwa mafano. Ndimo dinapatsa ie ntawi kuti
akatembenuza ntima; ndimo wosafuna ku tembenuza ntima
22 watshi kwa dama latshi. Ona, diponya ie m' kama, ndi
awo omwe atshita tshigololo nai' m' sautso yeikuru, kani
23 atembenuza ntima kwa ntshito zatshi. Ndimo didzapa ana
atshi ndi imfa; ndi maeklesia onse adzadziwa kuti diri ie
emwe asaka zintsukusana ndi mitima: ndimo didzapatsa
24 kwa onse a inu kwa ntshito zanu. Koma kwa inu dinena,
kwa omwe atsala m' Tiyatira, monga ambiri monga osali
ndi kupunzitsa kumene, omwe osadziwa zintu zakuya za
Satana, monga anena; sindiponya pa inu katundu wina.
25 Koma tshomwe mupotshera, gwirani kolimba kwa ntawi
26 difika. Ndi iemwe apambana, ndi iemwe asunga ntshito
zanga kwa nsonga, kwa ie didzapatsa mpamvu pa mitundu:
27 ndimo adzaweruza iyo ndi ntole ya tshitsulo, monga dziwira
dza waomba mbia dziswekedwa kwa mapale; monga anso
28 dalandira kwa Atatu anga: ndimo didzapatsa ie nyenyezi
29 ya mamawa. Iemwe ali kutu, amve tshomwe Nzimu unena
ndi maeklesia.
3 Ndi kwa njelo wa eklesia m' Sardis lemba;
Zintu zimenezi anena emwe apotshera Mizimu isanu ndi
iwiri ya Mulungu, ndi nyenyezi zisanu ndi ziwiri: didziwa
ntshito zako, kuti upotshera dzina kuti ukala ndi moyo,
2 ndimo uli wakufa. Kala wotshenjera, nulimbikitsa zintu
zomwe zitsala, zomwe zinatofuna ku fa: kuti dapeza palibe
ntshito za iwe zodzazidwa patsogolo pa Mulungu wanga.
3 Ndimo kumbukila bwanje walandira ndimo unamva; ndi
sunga, ndimo tembenuza ntima. Ndimo ngati usadzadikira,

didzadza monga woba, ndimo sudzadziwa ora liti didzadza
pa iwe. Koma upotshera maina owereng'jeka m' Sardis 4
omwe sanadetsa miinjiro yao: ndimo adzaendaenda ndi ine
m' zoyera; kuti aenera. Iemwe apambana adzabvekedwa 5
tshointsho m' miinjiro yoyera; ndimo sindidzafafaniza nditu
dzina latshi kwa buku la moyo, ndimo didzabvomereza dzina
latshi patsogolo pa Atatu anga, ndi patsogolo pa anjelo
atshi. Emwe ali kutu, amve tshomwe Nzimu unena ndi 6
maeklesia.

Ndimo kwa njelo wa eklesia m' Filadelfiya lemba; 7

Zintu zimenezi ati ie emwe ali woyera, iemwe ali woona,
iemwe apotshera fungulu ya Davide, iemwe atsegula, ndi
palibe modzi adzatseka, ndi emwe atseka, ndi palibe modzi
atsegula: didziwa ntshito zako (ona, dapatsa patsogolo pa iwe 8
tshitseko tshotsegudwa, tshomwe palibe modzi adziwa ku
tseka), kuti uli ndi mpamvu yeing'ono, ndi unasunga mau
anga, ndimo usanakana dzina langa. Ona, dipatsa kwa 9
sinagoge la Satana, a awo omwe anena ali Ayuda, ndimo
osali, koma anama; ona, didzapanga awo ku dza ndi ku
pembedza patsogolo pa mapazi ako, ndimo ku dziwa kuti
dakonda iwe. Tshifuka kuti unasunga mau a kulongosola 10
kwanga, ine enso didzasunga iwe kwa ora la kuyesa, *ora*
lidya lomwe lirikufika pa dziko lonse, ku yesa awo omwe
akala pa dziko. Didza nsanga: gwira kolimba tshomwe uli 11
natsho, kuti palibe modzi atshotse tshisoti tshotshuka tshako.
Iemwe apambana, didzapanga ie nzati m' malo oyera a 12
Mulungu wanga, ndimo sadzaturuka umo anso: ndimo
didzalemba pa ie dzina la Mulungu wanga, ndi dzina la
mzinda wa Mulungu wanga, Yerusalem watsopano, womwe
utsika kwa kumwamba kwa Mulungu wanga, ndi dzina langa
latsopano. Iemwe ali kutu, amve tshomwe Nzimu unena 13
ndi maeklesia.

Ndi kwa njelo wa eklesia m' Lawodikeya lemba; 14

Zintu zimenezi azinena Amen, womariza wamvanu ndi
woona, woiamba wa kupanga kwa Mulungu: Didziwa 15
ntshito zako, kuti usali kapena wozizira kapena wotenta:
difuna unali wozizira kapena wotenta. Tshointshi tshifuka 16
uli wofunda, ndimo *usali* kapena wotenta kapena wozizira,
didzasanza iwe mwa nkamwa mwanga. Tshifuka unena, 17
diri wolemera, ndimo dapotshera zolemera, ndimo sindifu-
nira kantu; ndimo wosadziwa kuti uli watshabe ndi
wazingalidwa ndi wosauka ndi wakungu ndi wamariseke:

18 diweruza iwe ku gula kwa ine golide linayepulidwa ndi
moto, kuti ungokala ndi zolemera; ndi miinjiro yoyera, kuti
ungobvala iwe eka, ndi *kuti* manyazi a mariseke ako
sangosonyezedwa; ndi mankwala a maso ku dzola maso
19 ako, kuti ungoona. Monga ambiri monga dikonda,
disulumula ndilanga : ndimo limbitsa, ndi tembenuza ntima.
20 Ona, diima pa tshitseko ndigogoda: ngati muntu modzi
amva liu langa ndimo atsegula tshitseko, didzaloa kwa ie,
21 ndidzadia nai', ndi ie ndi ine. Ie emwe apambana, didza-
patsa kwa ie ku kala pansi ndi ine m' mpando wotshuka
wanga, monga ine enso dinapambana, ndinakala pansi ndi
22 Atatu anga m' mpando wotshuka watshi. Iemwe ali kutu,
amve tshomwe Nzimu unena ndi maeklesia.

4 Pambuiu zintu zimenezi dinaona, ndimo ona, tshitseko
tshotsegulidwa m' mwamba, ndi liu loiamba lomwe dinamva,
*liu* monga la lipenga kulankula ndi ine, modzi kunena,
Kwera muno, ndimo didzasonyeza iwe zintu zomwe
2 zikanafika pambuiu. Tsopano lino dinali m' nzimu: ndimo
ona, mpando wotshuka unaukidwa m' mwamba, ndi
3 modzi kukala pa mpando wotshuka; ndi iemwe anakala *anali*
ku yang'anitsa wofana mwala wa yaspis ndi wa sardino: ndimo
*unali* utawalezi wozungulira mpando wotshuka, wofana ndi
4 smaradino ku yang'ana. Ndimo wozungulira mpando
wotshuka *inali* mipando yotshuka makumi awiri ndi inai:
ndi pa mipando yotshuka *dinaona* akuru makumi awiri
ndi anai kukala, abvekedwa m' miinjiro yoyera; ndi
5 pa mitu yao zisoti zotshuka za golide. Ndi kwa mpando
wotshuka zituruka zimpezi ndi maliu ndi mabingu. Ndimo
*inali* miuni isanu ndi iwiri ya moto kuaka patsogolo pa
mpando wotshuka, yomwe iri mizimu isanu ndi iwiri ya
6 Mulungu; ndimo patsogolo pa mpando wotshuka,
monga inali nyanja yaglase yofana ndi kristalo; ndimo
mkati mwa mpando wotshuka, ndi kozungulira mpando
wotshuka, zamoyo zinai zodzaza ndi maso patsogolo ndi
7 pambuiu. Ndi tshamoyo tshoiamba *tshinali* tshofana
mkango, ndi tshamoyo tshatshiwiri tshofana mwana wa
ng'ombe, ndi tshamoyo tshatshitatu tshinali ndi nkope
monga ya muntu, ndi tshamoyo tshatshinai *tshinali* tshofana
8 ndi tshombankanga tshouluka. Ndi zamoyo zinai, kuli
zonse ndi mapiko asanu ndi modzi, ziri zodzaza ndi maso
kozungulira ndi pakati: ndimo siziri ndi kupuma msana ndi
usiku, kuti, Woyera, woyera, woyera, *ali* Mwini Mulungu,

Wampamvuyonse, emwe anali ndi emwe ali ndi emwe adza.
Ndimo ntawi zamoyo zidzapatsa kupambana ndi ulemu ndi 9
tshakoma kwa iemwe akala pa mpando wotshuka, kwa
iemwe akala ndi moyo kwa magonero a magonero, akuru 10
makumi awiri ndi anai adzagwada patsogolo pa ie emwe
akala pa mpando wotshuka, ndimo adzapembedza ie emwe
akala ndi moyo kwa magonero a magonero, ndimo adza-
ponya zisoti zotshuka zao patsogolo pa mpando wotshuka,
kuti, Uli woenera, Mwini watu ndi Mulungu watu, ku 11
landira kupambana ndi ulemu ndi mpamvu: kuti unapanga
zintu zonse, ndi tshifuka tsha kufuna kwako zinali, ndimo
zinapangidwa.

Ndimo dinaona m' dzanja lamanja la emwe anakala pa 5
mpando wotshuka buku linalembedwa m' bwalo ndi kunja,
linasindikizidwa ndi zizindikilo zisanu ndi ziwiri. Ndimo 2
dinaona njelo wolimba kuuza ndi liu lalikuru, Ndani ali
woenera ku tsegula buku, ndi ku masula zizindikilo za ilo?
Ndimo palibe modzi m' mwamba, kapena pansi, kapena 3
pansi pa dziko, anali wolimba ku tsegula buku, kapena
ku yang'ana ilo. Ndimo dinalira misozi yambiri, tshifuka 4
palibe modzi wapezedwa woenera ku tsegula buku, kapena
ku yang'ana ilo: ndimo modzi wa akuru anena ndi ine, 5
Usalira nsozi: ona, Mkango womwe uli wa fuko la Yuda,
Ntsitsi wa Davide, wapambana, ku tsegula buku ndi
zizindikilo zisanu ndi ziwiri za ilo. Ndimo dinaona pakati 6
pa mpando wotshuka ndi *pakati* pa zamoyo zinai, ndi
pakati pa akuru, Mwana wa nkosa kuima, monga ngati
anapedwa, anali ndi nyanga zisanu ndi ziwiri, ndi maso
asanu ndi awiri, zomwe ziri mizimu isanu ndi iwiri ya
Mulungu, inatumidwa mwa dziko lonse. Ndimo anadza, 7
ndimo wa*li*tenga mwa dzanja lamanja la ie emwe nakala pa
mpando wotshuka. Ndimo ntawi anatenga buku, zamoyo 8
zinai ndi akuru makumi awiri ndi anai zinagwa patsogolo
pa Mwana wa nkosa, kupotshera zonse ndi maharpe, ndi
mbizi zagolide zodzaza ndi zonung'kira, zomwe ziri mapempero
a oyera. Ndimo ziimba nyimbo yatsopano, kuti, Woenera 9
uli iwe ku tenga buku, ndi ku tsegula zizindikilo za ilo:
kuti wapedwa, ndimo unagula kwa Mulungu ndi mwazi
wako *antu* a mafuko onse, ndi maliu, ndi antu, ndi mitundu,
ndimo unapanga awo *ku kala* kwa Mulungu watu dziko ndi 10
adzukuru; ndimo aweruza pa dziko. Ndimo dinaona, 11
ndinamva liu la anjelo ambiri kozungulira mpando wotshuka

ndi zamoyo ndi akuru; ndi kuwerenga kwa awo kunali
mazousan kumi opindulidwa ndi mazousan kumi, ndi
12 mazousan a mazousan; kuti ndi liu lalikuru, Woenera ali
Mwana wa nkosa emwe wapedwa ku landira mpamvu, ndi
zolemera, ndi nzeru, ndi kulimba, ndi ulemu, ndi kupambana,
13 ndi kudala. Ndimo zonse zopangidwa zomwe ziri m'
mwamba, ndi pansi, ndi pansi pa dziko, ndi pa nyanja, ndi
zintu zonse zomwe zirimo, dinamva kuti, Kwa ie emwe akala
pa mpando wotshuka, ndi pa Mwana wa nkosa, *zidzakale*
kudala, ndi ulemu, ndi kupambana, ndi kuweruza, kwa
14 magonero a magonero. Ndimo zamoyo zinai zinati, Amen.
Ndimo akuru nagwa napembedza.

6 Ndimo dinaona ntawi Mwana wa nkosa natsegula
tshimodzi tsha zizindikilo zisanu ndi ziwiri, ndinamva
tshimodzi tsha zamoyo zinai tshinena monga ndi liu la bingu,
2 Idza. Ndimo dinaona, ndi ona, kavalo woyera, ndi iemwe
nakala pa ie anali ndi uta; ndimo tshinapatsidwa kwa ie tshisoti
tshotshuka ndimo naturuka apambana, ndi ku pambana.
3 Ndimo ntawi natsegula tshizindikilo tshatshiwiri, dinamva
4 tshamoyo tshatshiwiri kunena, Idza. Ndimo *kavalo* wina
naturuka, kavalo wofira: ndimo kwa ie emwe nakala pa ie
kunapatsidwa ku tshotsa ntendere kwa dziko, ndimo kuti
akanapana: ndimo unapatsidwa kwa ie mpeni woukuru wa
nkondo.
5 Ndimo ntawi natsegula tshizindikilo tshatshitatu, dinamva
tshamoyo tshatshitatu kunena, Idza. Ndimo dinaona, ndi
ona, kavalo wakuda; ndimo iemwe nakala pa ie anali ndi
6 tshoyezera m' dzanja latshi. Ndimo dinamva monga linali
liu m' pakati pa zamoyo zinai kunena, Muyezo wa trigu
kwa denariyon, ndi miyezo itatu ya barle kwa denariyon;
ndi mafuta ndi vinyo usamwaza.
7 Ndimo ntawi anatsegula tshizindikilo tshatshinai, dinamva
8 liu la tshamoyo tshatshinai kunena, Idza. Ndimo dinaona,
ndi ona, kavalo woyezuka: ndi ie emwe nakala pa ie, dzina
latshi linali Imfa; ndi Hadesi natsata ndi iyo. Ndimo
kunapatsidwa kwa izo mpamvu pa pande latshinai la dziko,
ku pa ndi mpeni wa nkondo, ndimo ndi njala, ndimo ndi
imfa, ndimo ndi zirombo za dziko.
9 Ndimo ntawi natsegula tshizindikilo tshatshisanu, dinaona
pansi pa katshisi mizimu ya omwe anapedwa kwa mau a
10 Mulungu, ndi kwa kumariza komwe nasunga: ndimo
napfula ndi liu lalikuru, kunena, Ntawi yeitali bwanje, O

Mbuiye, woyera ndi woona, kodi usaweruza nusazimbula
mwazi watu pa awo omwe akala pa dziko? Ndimo kuna- 11
patsidwa awo kwa onse miinjiro yoyera; ndimo kunanenedwa
ndi awo, kuti akanapuma kosuntira kwa ntawi yeing'ono,
kwa ntawi akapolo anzao onso ndi abali ao, omwe akana-
pedwa inde monga anali, akanadzazidwa.

Ndimo dinaona ntawi anatsegula tshizindikilo tshatshisanu 12
ndi tshimodzi, ndimo tshinali tshibvomezi tshatshikuru; ndi
dzua linakala lakuda monga tshiguduli *tshakuda* tsha ubwea
*wa mbuzi*, ndi mwezi wonse unakala monga mwazi; ndi 13
nyenyezi za kumwamba zinagwa kwa dziko, monga ntengo
wa nkuyu utaia nkhuyu zatshi zosapsa, ntawi ugwedere-
dwa ndi mpepo yeikuru. Ndi kumwamba kunatshotsedwa 14
monga mputu ntawi upindidwa; ndi mapiri onse ndi dzisi
dzonse zinasuntidwa kwa malo ao. Ndimo mafumu otshuka 15
a dziko, ndi oweruza, ndi akazembe akuru, ndi olemera, ndi
olimba, ndi akapolo onse ndi aufulu onse, anabisala awo oka
m' mapanga ndi m' matantwe a mapiri; ndimo anena ndi 16
mapiri ndimo ndi matantwe, Igwani pa ife, ndimo bisani
ife kwa nkope ya iemwe akala pa mpando wotshuka, ndi
kwa kukwiira kwa Mwana wa nkosa: kuti siku lalikuru 17
la kukwiira kwao linafika; ndimo ndani adziwa ku ima?

Pambuiu pa tshimene dinaona anjelo anai kuima pa 7
ngondia zinai za dziko, kugwira mpepo zinai za dziko, kuti
palibe mpepo ikaomba pa dziko, kapena pa nyanja, kapena
pa ntengo umodzi. Ndimo dinaona njelo wina kukwera 2
kwa kuturuka kwa dzua, ali ndi tshizindikilo tsha Mulungu
wamoyo: ndimo napfula ndi liu lalikuru ku anjelo anai,
kwa omwe kunapatsidwa ku pweteka dziko ndi nyanja, kuti, 3
Musapweteka dziko, kapena nyanja, kapena mitengo, kwa
ntawi tasindikiza akapolo a Mulungu watu pa mpumi zao.
Ndimo dinamva kuwerenga kwa iwo omwe anasindikizidwa, 4
mazousan, makumi okaoka kumi, ndi makumi anai, ndi
anai asindikizidwa mwa mafuko onse a ana a Sirayeli.

A fuko la Yuda anasindikizidwa mazousan kumi ndi 5
awiri:
A fuko la Ruben mazousan kumi ndi awiri:
A fuko la Gadi mazousan kumi ndi awiri:
A fuko la Ashere mazousan kumi ndi awiri: 6
A fuko la Nafetali mazousan kumi ndi awiri:
A fuko la Manase mazousan kumi ndi awiri:
A fuko la Simon mazousan kumi ndi awiri: 7

A fuko la Levi mazousan kumi ndi awiri:
A fuko la Yisakare mazousan kumi ndi awiri:
8 A fuko la Zebulon mazousan kumi ndi awiri:
A fuko la Yosefe mazousan kumi ndi awiri:
A fuko la Benyamin anasindikizidwa mazousan kumi ndi awiri.

9 Pambuiu pa zintu zimenezi dinaona, ndi ona, antu ambiri,
omwe palibe muntu anadziwa ku werenga, mwa mitundu
yonse, ndi a mafuko *onse* ndi antu ndi maliu, kuima
patsogolo pa mpando wotshuka ndi patsogolo pa Mwana
wa nkosa, abvekedwa m' miinjiro yoyera, ndi ma-
10 kwata m' manja ao; ndimo apfula ndi liu lalikuru, kuti,
Kupulumutsa kwa Mulungu watu emwe akala pa mpando
11 wotshuka, ndi kwa Mwana wa nkosa. Ndimo anjelo onse
analikuima kozungulira mpando wotshuka, ndi *kozungulira*
akuru ndi zamoyo zinai; ndimo zinagwa patsogolo pa
mpando wotshuka pa nkope zao, ndimo zinapembedza
12 Mulungu, kuti, Amen: Kudala, ndi kupambana, ndi nzeru,
ndi kunena tshakoma, ndi ulemu, ndi mpamvu, ndi kuli-
mba, *zikale* kwa Mulungu watu kwa magonero a magonero.
13 Amen. Ndimo modzi wa akuru naiang'ka, kunena ndi ine,
Amene omwe abvekedwa m' miinjiro yoyera, ali ani, ndimo
14 anadzera kuti? Ndimo danena ndi ie, Mwini wanga,
udziwa. Ndimo nanena ndi ine, Amene ali awo omwe
aturuka mwa sautso yeikuru, ndimo natsuka miinjiro yao,
15 napanga iyo yoyera m' mwazi wa Mwana wa nkosa. Mwa
kuti ali patsogolo pa mpando wotshuka wa Mulungu; naimi-
rira ie msana ndi usiku m' tempile latshi: ndimo ie emwe
akala pa mpando wotshuka adzayala msasa watshi pa awo.
16 Sadzamva njala ntawi ina, kapena sadzamva ludzu ntawi
ina; kapena dzua silidzamenya pa awo, kapena tshitutu
17 tshina: kuti Mwana wa nkosa emwe ali pakati pa mpando
wotshuka adzakala mbusa wao, ndimo adzatsogolera awo
kwa akasope a madzi a moyo: ndimo Mulungu adzapukuta
misozi yonse kwa maso ao.

8 Ndimo ntawi anatsegula tshizindikilo tshisanu ndi tshi-
wiri, kunatsata kutontola m' mwamba kwa ntawi ya nusu
2 la ora. Ndimo dinaona anjelo asanu ndi awiri omwe aima
patsogolo pa Mulungu; ndimo anapatsidwa kwa awo
malipenga asanu ndi awiri.

3 Ndimo njelo wina nafika naima pa katshisi, kunali ndi
tshogwirira tsha zofukiza tshagolide; ndimo zinapatsidwa

kwa ie zofukiza zambiri, kuti akaziong'khetsa kwa mapempero a oyera onse pa katshisi wagolide emwe anali
patsogolo pa mpando wotshuka. Ndimo utsi wa zofukiza, 4
ndi mapempero a oyera, unakwera patsogolo pa Mulungu
mwa dzanja la anjelo. Ndimo anjelo watenga tshogwirira 5
tsha zonung'kira; ndimo natshidzaza ndi moto wa katshisi, naponya pa dziko: ndimo zinatsata mabingu, ndi maliu, ndi zimpezi, ndi tshibvomezi.

Ndimo anjelo asanu ndi awiri omwe anali ndi malipenga 6
asanu ndi awiri nadzikonza ku omba.

Ndimo woiamba naomba, ndimo zinatsata matalala ndi 7
moto, zosang'kanizidwa ndi mwazi, ndimo zinaponyedwa pa dziko: ndi pande latshitatu la dziko linaotshedwa, ndi pande latshitatu la mitengo linaotshedwa, ndi maudzu onse obiriwira anaotshedwa.

Ndimo njelo watshiwiri naomba, ndimo monga linali piri 8
lalikuru lipsa ndi moto linaponyedwa m' nyanja: ndi pande
latshitatu la nyanja linakala mwazi; ndimo linafa pande 9
latshitatu la zamoyo zomwe zinali m' nyanja, *inde* zomwe zinali ndi moyo; ndi pande latshitatu la dzombo linamwazidwa.

Ndimo njelo watshitatu naomba, ndimo inagwa kwa 10
mwamba nyenyezi yeikuru, kuaka kofana ndi muni, ndimo inagwa pa pande latshitatu la mitsinje, ndi pa akasope a
madzi; ndimo dzina la nyenyezi litshedwa Ntengo-woawa: 11
ndi pande latshitatu la madzi linakala ntengo-woawa; ndi antu ambiri anafa ndi madzi, tshifuka anapangidwa oawa.

Ndimo njelo watshinai naomba, ndi pande latshitatu la 12
dzua linamenyedwa, ndi pande latshitatu la mwezi, ndi pande latshitatu la zinyenyezi; kuti pande latshitatu la izo likadetsedwa, ndi msana sukawala kwa pande latshitatu la iwo, ndi usiku modzimodzi.

Ndimo dinaona, ndimo dinamva tshombankanga, ku- 13
uluka pakati pa mwamba, kunena ndi liu lalikuru, Tshaipa, tshaipa, tshaipa, kwa awo omwe akala pa dziko, ndi tshifukwa tsha maliu ena a lipenga la anjelo atatu, omwe kosuntira alikuomba.

Ndimo njelo watshisanu naomba, ndimo dinaona nyenyezi 9
kwa mwamba inagwa kwa dziko: ndimo inapatsidwa kwa
ie fungulu ya dzenje la phompo. Ndimo natsegula dzenje 2
la phompo; ndimo utsi unakwera kwa dzenje, monga utsi wa ng'anjo yeikuru; ndimo dzua ndi mlengalenga zinade-

3 tsedwa tshifuka tsha utsi wa dzenje. Ndimo mwa utsi
anaturuka madzombe pa dziko; ndimo mpamvu inapatsidwa
kwa awo, monga dzing'kanira dza dziko dzipotshera mpa-
4 mvu. Ndimo ananenedwa ndi awo kuti sakapwetekesa udzu
wa dziko, kapena kantu kobiriwira, kapena ntengo wina,
koma koka antu otere omwe osali ndi tshizindikilo tsha
5 Mulungu pa mpumi zao. Ndimo anapatsidwa kwa awo
kuti sakapa awo, koma kuti akazunzidwa miezi isanu:
ndimo kuzunza kwao kunali monga kuzunza kwa tshing'ka-
6 nira, ntawi tshiluma muntu. Ndimo m' masiku adya antu
adzafuna imfa, ndimo sadzaipeza nditu; ndimo adzafuna
7 ku fa, ndimo imfa itawa kwa awo. Ndimo makalidwe a
madzombe anali ofana ndi akavalo okonzetsedwa kwa
nkondo; ndimo pa mitu yao monga zinali zisoti zotshuka
zofana ndi golide, ndimo nkope zao zinali monga nkope za
8 antu. Ndimo anali ndi tsisi monga tsisi la akazi, ndi mano
9 ao anali monga *mano* a mikango. Ndimo anali ndi zotshi-
njiriza, monga zinali zotshinjiriza za tshitsulo; ndimo
namalowe wa mapiko ao anali monga namalowe wa matsha-
riote, wa akavalo ambiri kutamanga nsanga kwa nkondo.
10 Ndimo anali ndi mitshira yofana ndi zing'kanira, ndi
zimbola; ndimo m' mitshira yao iri mpamvu yao ku
11 pwetekesa antu miezi isanu. Apotshera pambana pao monga
fumu yotshuka njelo wa phompo: dzina latshi m' Tshihe-
bere liri Abadon, ndimo m' Tshigrike ali ndi dzina
Apoliyon.
12 Tshaipa tshoiamba tshinapita: ona, zirinkudza kosuntira
Zoipa zina ziwiri pambuiu.
13 Ndimo njelo watshisanu ndi tshimodzi naomba, ndimo
dinamva liu kwa nyanga za katshisi wagolide emwe ali
14 patsogolo pa Mulungu, modzi kunena ndi njelo watshisanu
ndi tshimodzi, emwe anali ndi lipenga, Masula anjelo anai
15 omwe amangidwa pa ntsinje woukuru Ferate. Ndimo
anjelo anai anamasulidwa, omwe anafotokozedwa kwa ora ndi
siku ndi mwezi ndi tshaka, kuti akapa pande latshitatu la
antu.
16 Ndimo kuwerenga kwa magulu a ankhondo a antu pa
akavalo kunali kawiri, mazousan kumi opindulidwa ndi
17 mazousan kumi: dinamva kuwerenga kwa awo. Ndimo
tshointsho dinaona akavalo m' tshoona, ndi awo omwe
anakala pa awo, anali ndi zotshinjiriza *monga* za moto ndi
za huakintos ndi za sulfure: ndi mitu ya akavalo iri yofana

mitu ya mikango; ndi mwa nkamwa mwao zituruka moto
ndi utsi ndi sulfure. Ndi dzaola dzitatu dzimenedzi pande 18
latshitatu la antu linapedwa, ndi moto ndi utsi ndi sulfure,
zomwe zinaturuka mwa nkamwa mwao. Kuti mpamvu ya 19
akavalo iri m' nkamwa mwao, ndi m' mitshira yao: kuti
mitshira yao iri yofana ndi zinjoka, ndimo ipotshera mitu;
ndimo ndi iyo apweteka. Ndimo otsala a antu, omwe 20
sanapedwa ndi dzaola dzimenedzi, sanatembenuza ntima
kwa ntshito za manja ao, kuti sakapembedza ademon, ndi
mafano a golide, ndi a silivere, ndi a nkua, ndi a mwala,
ndi a ntengo; omwe osadziwa kapena ku ona, kapena ku
mva, kapena ku enda: ndimo sanatembenuza ntima kwa 21
mbanda zao, kapena kwa amabisalira ao, kapena kwa dama
lao, kapena kwa maumbala ao.

Ndimo dinaona njelo wina wolimba kutsika kwa ku- 10
mwamba, kubvekedwa ndi ntambo; ndi utawalezi unali pa
mutu watshi, ndi nkope yatshi inali yofana dzua, ndi
mapazi atshi ofana ndi mizati ya moto; ndimo napotshera 2
m' dzanja latshi buku laling'ono lotsegula: ndimo naika
pazi latshi lamanja pa nyanja, ndi lamanzere latshi pa
dziko; ndimo napfula ndi liu lalikuru, monga nkango 3
ubulira: ndimo ntawi nabulira, mabingu asanu ndi awiri
natshula maliu ao. Ndimo ntawi mabingu asanu ndi awiri 4
natshula *maliu ao*, dinatofuna ku lemba: ndimo dinamva
liu kwa kumwamba kunena, Sindikiza zintu zomwe mabingu
asanu ndi awiri anatshula, nusadzalemba izo. Ndimo njelo 5
emwe dinaona kuima pa nyanja ndi pa dziko natukula
dzanja latshi lamanja ku mwamba, nalumbira ndi ie emwe 6
akala ndi moyo kwa magonero a magonero, emwe napanga
kumwamba ndi zintu zomwe ziri momo, ndi dziko ndi zintu
zomwe ziri momo, ndi nyanja ndi zintu zomwe ziri momo,
kuti kusadzakala ntawi yopambana: koma m' masiku a liu 7
la njelo watshisanu ndi tshiwiri, ntawi atofuna ku omba,
pomwe kutedwa kusadziwitsa kwa Mulungu, kwa makalidwe
abwino omwe anauzidwa ku akapolo atshi aprofeti.
Ndimo liu lomwe dinamva kwa kumwamba, *dinalimva* anso 8
kulankula ndi ine, ndi kuti, Muka, tenga buku lomwe litse-
gulidwa m' dzanja la njelo emwe aima pa nyanja ndi pa
dziko. Ndimo dinamuka ku njelo, kunena ndi ie kuti 9
akapatsa kwa ine buku laling'ono. Ndimo anena ndi ine,
Tenga ilo, nulidia; ndimo lidzaawitsa mimba yako, koma
m' nkamwa mwako lidzakala lotsetshemera monga utshi.

10 Ndimo dinatenga buku laling'ono mwa dzanja la njelo,
ndinalidia; ndimo linali m' nkamwa mwanga lotsetshemera
monga utshi: ndimo ntawi dinalidia, mimba yanga inaawi-
11 tsidwa. Ndimo anena ndi ine, Ukanalosa auso ndi antu
ambiri ndi mitundu ndi maliu ndi mafumu otshuka.
11 Ndimo kunapatsidwa kwa ine nzengo yofana ndi ntole:
ndimo modzi anati, Uka, nulinganiza tempile la Mulungu,
2 ndi katshisi, ndi awo omwe apembedza momo. Ndimo
bwalo lomwe liri kunja la tempile sia kunja, ndimo usalili-
nganiza; kuti linapatsidwa kwa mitundu: ndimo mzinda
woyera adzauponda pansi pa pazi miezi makumi anai ndi
3 iwiri. Ndimo didzapatsa kwa omariza anga awiri, ndimo
adzalosa masiku zousan, mazana awiri ndi makumi asanu
4 ndi modzi, obvekedwa ndi tshiguduli. Amene ali mitengo
yaolive iwiri ndi zogwirira nyali ziwiri, kuima patsogolo
5 pa Mwini wa dziko. Ndimo ngati muntu modzi afuna ku
pweteka awo, moto uturuka kwa nkamwa mwao, numwaza
maliwongo ao: ndimo ngati muntu modzi adzafuna ku
6 pweteka awo, tshointshi akanapedwa. Amene ali ndi
mpamvu ku tseka mwamba, kuti sikuvumba m' masiku a
kulosa kwao: ndimo anali ndi mpamvu pa madzi ku tembe-
nuza awo ku mwazi, ndi ku menya dziko ndi dzaola dzonse,
7 ntawi zambiri monga adzafuna. Ndimo ntawi anata ku-
mariza kwao, nyama yomwe ikwera mwa phompo idzapanga
nkondo ndi awo, ndimo idzapambana awo, nidzápa awo.
8 Ndimo mitembo yao *ikala* m' kwalala la mzinda woukuru,
womwe wanzimu utshedwa Sodom ndi Yiputa, pomwe enso
9 Mwini wao anapatshikidwa. Ndimo kwa antu ndi mafuko
ndi maliu ndi mitundu *antu* alikuyang'anira pa mitembo yao
masiku atatu ndi nusu, ndimo osaleka mitembo yao ku
10 ikidwa m' mwanda. Ndimo awo omwe akala pansi ako-
ndwera pa awo, nasekera; ndimo adzatumiza zaulere modzi
kwa wina; tshifuka aprofeti awiri amene nasautsa awo
11 omwe akala pansi. Ndimo pambuiu masiku atatu ndi nusu
pwea la moyo kwa Mulungu linaloa mwa awo, ndimo
naima pa mapazi ao; ndimo kuopa kwambiri kunagwa pa
12 awo omwe naona awo. Ndimo anamva liu lalikuru kwa
kumwamba kunena ndi awo, Kwerani kuno. Ndimo na-
kwera m' mwamba m' ntambo; ndimo maliwongo ao naona
13 awo. Ndimo m' ora limene tshinali tshibvomezi tshatshi-
kuru, ndi pande kumi la mzinda linagwa; ndimo anapedwa
m' tshibvomezi antu mazousan asanu ndi awiri: ndimo

otsala anaopsedwa, napatsa kupambana kwa Mulungu wa
kumwamba.
Tshaipa tshatshiwiri tshinapita: ona, Tshaipa tshatshitatu 14
tshifika nsanga.
Ndimo njelo watshisanu ndi tshiwiri naomba; ndimo na- 15
tsata maliu akuru m' mwamba, ndimo nati, Dziko la dziko
lonse linafika *dziko* la Mwini watu, ndi la Kristu watshi:
ndimo adzaweruza kwa magonero a magonero. Ndimo 16
akuru makumi awiri, ndi anai, omwe akala patsogolo pa
Mulungu pa mipando yotshuka yao, nagwa pa nkope zao,
napembedza Mulungu, kuti, Tipatsa tshakoma kwa iwe, O 17
Mwini Mulungu, Wampamvuyonse, emwe uli ndi emwe
unali; tshifuka watenga mpamvu yako yeikuru, ndi una-
weruza. Ndimo mitundu inakwiira, ndimo kukwiira kwako 18
kunafika, ndi ntawi ya akufa ku weruzidwa, ndi *ntawi*
ku patsa kulipira kwao ku akapolo ako aprofeti, ndi kwa
oyera, ndi kwa awo omwe aopa dzina lako, ang'ono ndi
akuru; ndi ku mwaza awo omwe amwaza dziko.
Ndimo kunatsegulidwa tempile la Mulungu lomwe liri m' 19
mwamba; ndimo kunaonedwa m' tempile latshi arke la
kupangana kwatshi; ndimo zinatsata zimpezi, ndi maliu,
ndi mabingu, ndi tshibvomezi, ndi matalala akuru.
Ndimo tshizindikilo tshatshikuru tshinaonedwa m' mwa- 12
mba; nkazi abvekedwa ndi dzua, ndi mwezi pansi pa
mapazi atshi, ndi pa mutu watshi tshisoti tshotshuka tsha
nyenyezi kumi ndi ziwiri; ndimo anali ndi mimba: ndimo 2
apfula, kubala, ndimo m' ululu ku balidwa. Ndimo tshina- 3
onedwa tshizindikilo tshina m' mwamba; ndimo ona, nsatu
yeikuru yofira, kuli ndi mitu isanu ndi iwiri ndi nyanga
kumi, ndi pa mitu yatshi madiadema asanu ndi awiri.
Ndimo ntshira watshi ukoka pande latshitatu la nyenyezi 4
za kumwamba ndi unaponya izo pansi: ndimo nsatu inaima
patsogolo pa nkazi emwe anatofuna ku bala, kuti ntawi
anabala, anangomwaza mwana watshi. Ndimo anabala 5
mwana, mwana wamamuna, emwe adzaweruza mitundu
yonse ndi ntole ya tshitsulo: ndimo mwana watshi anatuku-
lidwa kwa Mulungu, ndi kwa mpando wotshuka watshi.
Ndimo nkazi natawira m' tshipululu, pomwe wapotshera 6
malo ofotokozedwa ndi Mulungu, kuti apo angolera ie
masiku zousan mazana awiri ndi makumi asanu ndi modzi.
Ndimo kunali nkondo m' mwamba: Mikayeli ndi anjelo 7
atshi *analikuturuka* kwa nkondo ndi nsatu; ndimo nsatu

8 inapanga nkondo ndi anjelo atshi; ndimo sanapambana,
kapena malo ao sanapezedwa ntawi ina m' mwamba.
9 Ndimo nsatu yeikuru inaponyedwa pansi, njoka yeikali,
yomwe itshedwa Diabolos ndi Satana, yonyenga ya dziko
lonse; inaponyedwa pansi, ndi anjelo atshi anaponyedwa
10 pansi nayo. Ndimo dinamva liu lalikuru m' mwamba,
kuti, Tsopano zinafika kupulumutsa, ndi mpamvu, ndi dziko
la Mulungu watu, ndi kuweruza kwa Kristu watshi: kuti
wotshula wa abali atu aponyedwa pansi, emwe atshula awo
11 patsogolo pa Mulungu watu msana ndi usiku. Ndimo
napambana ie tshifuka tsha mwazi wa Mwana wa nkosa,
ndi tshifuka tsha mau a kumariza kwao; ndimo sanakonda
12 moyo wao inde kwa imfa. Ndimo sekerani, O miamba, ndi
inu nomwe mukala mwa iyo. Tshaipa kwa dziko ndi kwa
nyanja: tshifuka diabolos anatsika kwa inu, ali ndi kukwiira
kwakukuru, kudziwa kuti ali ndi ntawi yeing'ono nditu.
13 Ndimo ntawi nsatu inaona kuti inaponyedwa pansi,
14 inazunza nkazi emwe anabala *mwana* wamamuna. Ndimo
kunapatsidwa kwa nkazi mapiko awiri a tshombankanga
tshatshikuru, kuti anangouluka m' tshipululu ku malo
atshi, pomwe aleredwa kwa ntawi, ndi zintawi, ndi nusu la
15 ntawi, kwa nkope ya njoka. Ndimo njoka inaturutsa mwa
nkamwa mwatshi pambuiu nkazi madzi monga ntsinje, kuti
16 anangopanga ie ku kokoledwa ndi ntsinje. Ndimo dziko
linatangata nkazi, ndi dziko linatsegula nkamwa mwatshi,
ndimo linameza ntsinje womwe nsatu inaturutsa mwa
17 nkamwa mwatshi. Ndimo nsatu inakwiira ndi nkazi, ndimo
inamuka ku panga nkondo ndi yotsala ya mbeu yatshi,
yomwe isunga mau a Mulungu, nisunga kumariza kwa Yesu:
13 ndimo inaima pa ntshenga wa nyanja.

Ndimo dinaona nyama kuturuka mwa nyanja, iri ndi
nyanga kumi ndi mitu isanu ndi iwiri, ndi pa nyanga zatshi
madiadema kumi, ndi pa mitu yatshi maina a kutukwana.
2 Ndimo nyama yomwe dinaona inafana ndi nialugwi, ndi
mapazi atshi anali monga *mapazi* a bera, ndimo nkamwa
mwatshi monga nkamwa mwa nkango: ndimo nsatu inapatsa
iyo mpamvu yatshi, ndi mpando wotshuka watshi, ndi
3 kuweruza kwakukuru. Ndimo *dinaona* umodzi wa mitu
yatshi monga ngati unamenyedwa kwa imfa; ndimo
nkakato-wa-imfa watshi unatshiritsidwa: ndi dziko lonse
4 linazizwa pambuiu pa nyama; ndimo anapembedza nsatu,
tshifuka inapatsa kuweruza kwatshi kwa nyama; nape-

mbedza nyama, kuti, Ndani ali wofana ndi nyama? ndimo
ndani adziwa ku panga nkondo ndi iyo? ndimo kunapa- 5
tsidwa kwa iyo nkamwa kulankula zintu zazikuru ndi matu-
kwano; ndimo kunapatsidwa kwa iyo kuweruza ku kalabe
miezi makumi anai ndi iwiri. Ndimo inatsegula nkamwa 6
mwatshi kwa matukwano pa Mulungu, ku tukwana dzina
latshi, ndi msasa watshi, *inde* awo omwe akala m' mwamba.
Ndimo kunapatsidwa kwa iyo ku panga nkondo ndi oyera, 7
ndi ku pambana awo: ndimo kunapatsidwa ku iyo kuweruza
pa mafuko onse ndi antu ndi maliu ndi mitundu. Ndimo 8
onse omwe akala pa dziko adzapembedza iyo, *onse* maina a
omwe sanalembedwa m' buku la moyo la Mwana wa nkosa
emwe wapedwa kwa kuzika kwa dziko. Ngati muntu 9
modzi ali kutu, amve. Ngati muntu modzi *ali* kwa ukoli, 10
mwa ukoli apita: ngati muntu modzi adzapa ndi mpeni
wankondo, ndi mpeni wankondo akanapedwa. Muno ziri
kulongosola ndi mvanu za oyera.

Ndimo dinaona nyama ina ituruka mwa pansi; ndimo inali 11
ndi nyanga ziwiri zofana ndi mwana wa nkosa, ndimo ina-
lankula monga nsatu. Ndimo itshita kuweruza konse kwa 12
nyama yoiamba m' kuona kwatshi. Ndimo ipanga dziko
ndi awo omwe akala momo ku pempedza nyama yoiamba,
nkakato-wa-imfa wa yomwe unatshiritsidwa. Ndimo itshita 13
zizindikilo zazikuru, kuti inde ikanatsitsa moto kwa mwamba
pansi m' kuona kwa antu. Ndimo inyenga awo omwe akala 14
pansi ndi tshifukwa tsha zizindikilo zomwe zinapatsidwa
kwa iyo ku tshita m' kuona kwa nyama; kunena ndi awo
omwe akala pansi, kuti akapanga fanizo kwa nyama, yomwe
iri ndi nkakato-wa-mpeni wa nkondo, ndimo inakala ndi
moyo. Ndimo kunapatsidwa *kwa iyo* ku patsa pwea kwa ilo, 15
*inde* kwa fanizo la nyama, kuti fanizo la nyama likalankula,
ndi lipanga kuti monga ambiri monga sakanapembedza
fanizo la nyama akapedwa. Ndimo ipanga onse, ang'ono 16
ndi akuru, ndi olemera ndi osauka, ndi aufulu ndi akapolo,
kuti kupatsidwa kwa awo lemba pa dzanja lamanja lao,
kapena pa pumi zao; ndimo kuti palibe muntu akadziwa ku 17
gula kapena ku gulitsa, kapena iemwe ali ndi lemba, *inde*
dzina la nyama kapena kuwerenga kwa dzina latshi. Pano 18
ziripo nzeru. Iemwe ali ndi kudziwitsa, awerenge kuwere-
nga kwa nyama; kuti kuli kuwerenga kwa muntu: ndi
kuwerenga kwatshi kuli Mazana asanu ndi modzi, ndi
makumi asanu ndi modzi, ndi asanu ndi modzi.

14 Ndimo dinaona, ndi ona, Mwana wa nkosa kuima pa
piri la Ziyon, ndimo ndi ie mazousan, makumi okaoka
kumi, ndi makumi anai ndi anai, ali ndi dzina latshi, ndi
2 dzina la Atatu atshi, analembedwa pa pumi zao. Ndimo
dinamva liu kwa kumwamba, monga liu la madzi ambiri,
ndi monga liu la bingu lalikuru: ndi liu lomwe dinamva
3 *linali* monga *liu* la aharpe kuomba maharpe ao: ndimo
aimba monga inali nyimbo yatsopano patsogolo pa mpando
wotshuka, ndi patsogolo pa zamoyo zinai ndi akuru: ndimo
palibe muntu anadziwa ku punzira nyimbo koma mazousan,
makumi okaoka kumi ndi makumi anai, ndi anai, *inde* awo
4 omwe anagulidwa mwa pansi. Amene ali awo omwe sana-
detsedwa ndi akazi; kuti ali auweta. Amene *ali* omwe
atsata Mwana wa nkosa pomwe apita. Amene anagulidwa
kwa mwa antu, *ku kala* dzobala dzoiamba kwa Mulungu ndi
5 kwa Mwana wa nkosa. Ndimo m' nkamwa mwao linapeze-
dwa palibe bodza: ali opanda kalama.
6 Ndimo dinaona njelo wina kuuluka mkati mwamba,
kupotshera ivangeli wosamariza ku uza kwa awo omwe
akala pa dziko, ndi kwa mitundu yonse ndi mafuko
7 ndi maliu ndi antu; ndimo anena ndi liu lalikuru, Opani
Mulungu, ndimo patsani ie kupambana; kuti ora la kuwe-
ruza kwatshi linafika: ndimo pembedzani ie emwe napanga
kumwamba ndi pansi ndi nyanja ndi akasope a madzi.
8 Ndi wina, njelo watshiwiri, natsata, kuti, Unagwa, unagwa
Babilon wang'kuru, womwe wapanga mitundu yonse ku
mwa ndi vinyo wa kukwiira kwa dama latshi.
9 Ndimo njelo wina, watshitatu, natsata awo, kuti ndi liu
lalikuru, Ngati muntu modzi apembedza nyama ndi fanizo
latshi, nalandira lemba pa pumi yatshi, kapena pa dzanja
10 latshi, ie enso adzamwa ndi vinyo wa kukwiira kwa Mulungu,
emwe anafotokozedwa wosasang'kanizidwa m' tshiko tsha
kukwia kwatshi; ndimo adzazunzidwa ndi moto ndi sulfure
m' kuona kwa anjelo oyera, ndi m' kuona kwa Mwana wa
11 nkosa: ndimo utsi wa kuzunza kwao ukwera kwa magonero
a magonero; ndimo osapotshera kupuma msana ndi usiku,
awo omwe apembedza nyama ndi fanizo latshi, ndi iemwe
12 alandira lemba la dzina latshi. Pano pali kulongosola kwa
oyera, awo omwe asunga mau a Mulungu, ndi mvanu wa
Yesu.
13 Ndimo dinamva liu kwa kumwamba kuti, Lemba, Odala
ali akufa omwe afa m' Mwini kwa ntawi yatsopano: inde,

unena Nzimu, kuti angopuma kwa ntshito zao; kuti ntshito zao zitsata nao.

Ndimo dinaona, ndi ona, ntambo woyera; ndi pa 14
ntambo *dinaona* modzi kukala wofana ndi mwana wa muntu,
kupotshera pa mutu watshi tshisoti tshotshuka tshagolide,
ndimo m' dzanja latshi sekile lakutwa. Ndimo njelo wina 15
naturuka kwa tempile, kupfula ndi liu lalikuru kwa iemwe
anakala pa ntambo, Tumiza sekile lako, nutema: kuti ora
ku tema lafika; kuti masika a pansi ali ouma. Ndimo ie 16
emwe anakala pa ntambo naponya sekile latshi pa dziko;
ndi dziko linatemedwa.

Ndimo njelo wina naturuka kwa tempile lomwe liri m' 17
mwamba, ie enso kupotshera sekile lakutwa. Ndimo njelo 18
wina naturuka kwa katshisi, ie emwe ali ndi mpamvu pa
moto; ndimo napfula ndi liu lalikuru kwa iemwe anali ndi
sekile lakutwa, kuti, Turutsa sekile lako lakutwa, nukung'ka
matsango a mvina la dziko; kuti magrepe atshi ali oopsetsa.
Ndimo njelo naponya sekile latshi m' dziko, nakung'ka 19
mvina wa dziko, nauponya m' tshiwira tsha mvina, *tshiwira*
tshatshikuru, tsha kukwiira kwa Mulungu. Ndimo tshiwira 20
tshinapendedwa kunja kwa mzinda, ndimo unaturuka
mwazi kwa tshiwira, inde kwa makwerekwere a akavalo,
monga kutali monga mastadia zousan ndi mazana asanu ndi
modzi.

Ndimo dinaona tshizindikilo tshina m' mwamba, 15
tshatshikuru ndi tshozizwa, anjelo asanu ndi awiri ali ndi
dzaola dzisanu ndi dziwiri, *dzomwe dziri* dzakutungo, kuti
mwa idzo kunata kukwiira kwa Mulungu.

Ndimo dinaona monga kunali nyanja yaglase yosang'kani- 2
zidwa ndi moto; ndi awo omwe adza opambana kwa
nyama, ndi kwa fanizo latshi, ndi kwa kuwerenga kwa dzina
latshi, kuima ndi nyanja yaglase, kuli ndi maharpe a
Mulungu. Ndimo aimba nyimbo ya Moses kapolo wa 3
Mulungu, ndi nyimbo ya Mwana wa nkosa, kunena,
Zazikuru ndi zozizwa ziri ntshito zako, O Mwini Mulungu,
Wampamvuyonse; zodeka ndi zoona ziri njira zako, iwe
Fumu Yotshuka ya magonero. Ndani sadzaopa, O Mwini, 4
ndi sadzapambanitsa dzina lako? kuti iwe eka uli woyera;
kuti mitundu yonse idzafika ndimo idzapembedza patsogolo
pa iwe; kuti ntshito zako zodeka zinasonyezedwa.

Ndimo pambuiu zintu zimenezi dinaona, ndimo tempile 5
la msasa wa kumariza m' mwamba linatsegulidwa: ndimo 6

naturuka kwa tempile anjelo asanu ndi awiri omwe anali
ndi dzaola dzisanu ndi dziwiri, abvekedwa ndi mwala
*wolemera*, woyera *ndi* wowala, namangira pa maere ao ndi
7 malamba agolide. Ndimo tshimodzi tsha zamoyo zinai tshi-
napatsa kwa anjelo asanu ndi awiri mbizi zisanu ndi ziwiri
zagolide zodzaza ndi kukwiira kwa Mulungu, emwe akala ndi
8 moyo kwa magonero a magonero. Ndimo tempile linadzazi-
dwa ndi utsi kwa kupambana kwa Mulungu, ndi kwa mpamvu
yatshi; ndimo palibe modzi anadziwa ku loa m' tempile,
kwa ntawi dzaola dzisanu ndi dziwiri dza anjelo asanu ndi
awiri dzikatedwa.

16 Ndimo dinamva liu lalikuru mwa tempile, kuti ku anjelo
asanu ndi awiri, Mukani, mutsanula zimbizi zisanu ndi ziwiri
za kukwiira kwa Mulungu m' dziko.

2 Ndimo woiamba namuka, natsanula mbizi yatshi m' dziko; ndimo tshinakala tshironda tshonyansa ndi tsholemera pa antu omwe anali ndi lemba la nyama, ndi omwe napembedza fanizo latshi.

3 Ndimo watshiwiri natsanula mbizi yatshi m' nyanja; ndimo tshinakala mwazi monga wa muntu wakufa; ndi mizimu yonse yamoyo inafa, *inde* zintu zomwe zinali m' nyanja.

4 Ndimo watshitatu natsanula mbizi yatshi m' mitsinje ndi
5 m' akasope a madzi; ndimo tshinakala mwazi. Ndimo
dinamva njelo wa madzi kunena, Wodeka uli iwe, emwe uli
ndi emwe unali, Woyera iwe, tshifuka unaweruza tshointshi:
6 kuti anatsanula mwazi wa oyera ndi aprofeti, ndimo mwazi
7 unapatsa awo ku mwa: ali oenera. Ndimo dinamva
katshisi kuti, Inde, O Mwini Mulungu, Wampamvuyonse,
oona ndi odeka ali maweruzo ako.

8 Ndimo watshinai anatsanula mbizi yatshi pa dzua; ndimo
9 kunapatsidwa kwa ilo ku otsha antu ndi moto. Ndimo antu
anaotshedwa ndi kutenta kwambiri: ndimo natukwana
dzina la Mulungu emwe anali ndi mpamvu pa dzaola
dzimenedzi; ndimo sanatembenuza ntima ku patsa ie
kupambana.

10 Ndimo watshisanu natsanula mbizi yatshi pa mpando
wotshuka wa nyama; ndimo dziko latshi linadetsedwa;
11 ndimo anatafuna malilume ao ndi ululu, ndimo natukwana
Mulungu wa mwamba tshifuka tsha maululu ao ndi
zironda zao; ndimo sanatembenuza ntima ndi ntshito zao.

12 Ndimo watshisanu ndi tshimodzi anatsanula mbizi yatshi
pa ntsinje woukuru, *ntsinje* Ferate; ndimo madzi a iwo

anaumidwa, kuti njira inangopangidwa yakuta kwa mafumu
otshuka omwe *afika* kwa kuturuka kwa dzua. Ndimo 13
dinaona *kuturuka* kwa nkamwa mwa nsatu, ndi kwa
nkamwa mwa nyama, ndi kwa nkamwa mwa mprofeti
wonyenga, mizimu itatu yosatsuka, monga anali atshule:
kuti inali mizimu ya ademon, kutshita zizindikilo; yomwe 14
ituruka kwa mafumu otshuka a dziko lonse, ku song'kana
awo kwa nkondo ya siku lalikuru la Mulungu, Wampamvu-
yonse. (Ona, difika monga woba. Wodala ali iemwe 15
adikira, nasunga miinjiro yatshi, kani aenda womariseke,
ndimo aona manyazi atshi.) Ndimo nasong'kanitsa awo m' 16
malo omwe atshedwa m' Tshihebere Har-Magedon.

Ndimo watshisanu ndi tshiwiri natsanula mbizi yatshi pa 17
mlengalenga; ndimo linaturuka liu lalikuru kwa tempile,
kwa mpando wotshuka, kunena, Tshata: ndimo zinali zi- 18
mpezi, ndi maliu, ndi mabingu; ndimo tshinali tshibvomezi
tshatshikuru, tshotere monga sitshinali kwa ntawi anali antu
pa dziko, tshibvomezi tshatshikuru tshotere, tsholimba
tshotere. Ndi mzinda woukuru unagawidwa m' mapande 19
atatu, ndi mizinda ya mitundu inagwa: ndi Babilon wou-
kuru unakumbukidwa m' kuona kwa Mulungu, ku patsa
ku iwo tshiko tsha vinyo wa nkarwe ya kukwiira kwatshi.
Ndimo dzisi dzonse dzinatawa, ndi mapiri sanapezedwa. 20
Ndimo matalala akuru, *miala yonse umodzi ndi umodzi* pa 21
kulemera kwa talente, atsika kwa kumwamba pa antu:
ndimo antu natukwana Mulungu tshifuka tsha tshaola
tsha matalala; kuti tshaola tsha awo tshiri tshatshikuru
tshambiri.

Ndimo anadza modzi wa anjelo asanu ndi awiri omwe 17
anapotshera mbizi zisanu ndi ziwiri, nalànkula ndi ine, kuti,
Idza kuno, didzasonyeza iwe kuweruza kwa nkazi wa dama
wang'kuru emwe akala pa madzi ambiri; ndi emwe mafumu 2
otshuka a dziko anatshita dama, ndimo awo omwe akala m'
dziko analedzedwa ndi vinyo wa dama latshi. Ndimo nanya- 3
mula ine mu Nzimu m' tshipululu: ndimo dinaona nkazi
kukala pa nyama yofira, yodzaza ndi maina a kutukwana,
iri ndi mitu isanu ndi iwiri ndi nyanga kumi. Ndimo nkazi 4
wabvekedwa ndi zakuda ndi zofira, nabvaliridwa ndi golide
ndi miala yolemera ndi maperile, kupotshera m' dzanja latshi
tshiko tshagolide tshodzaza ndi zonyansa, inde zintu zosa-
tsuka za dama latshi, ndi pa pumi yatshi dzina lolembedwa, 5
KUSADZIWIKA, BABILON WANG'KURU, AMAI A AKAZI A DAMA NDI

6 a zonyansa za dziko. Ndimo diuaona nkazi woledzedwa
ndi mwazi wa oyera, ndimo ndi mwazi wa omariza a Yesu.
Ndimo ntawi dinaona ie, dinazizwa ndi kuzizwa kwakukuru.
7 Ndimo njelo nanena ndi ine, Nanga bwanje unazizwa?
Didzauza iwe kusadziwika kwa nkazi, ndi kwa nyama
yomwe inyamula ie, yomwe iri ndi mitu isanu ndi iwiri ndi
8 nyanga kumi. Nyama yomwe unaona inali, ndimo siiri;
ndimo itofuna ku turuka kwa phompo, ndi ku muka kwa
kumwaza. Ndimo awo omwe akala pa dziko adzazizwa,
*awo* maina a omwe sanalembedwa m' buku la moyo kwa
kuzika kwa dziko, ntawi aona nyama, bwanje kuti inali, ndi
9 siiri, ndimo idzafika. Pano uli muwongo womwe upotshera
nzeru. Mitu isanu ndi iwiri iri mapiri asanu ndi awiri,
10 pomwe nkazi akala: ndimo ali mafumu otshuka asanu
ndi awiri; asanu anagwa, imodzi iri, ina siinafika kosuntira;
11 ndimo ntawi ifika, ikanakalabe ntawi yeing'ono. Ndimo
nyama yomwe inali, ndi siiri, iri iyo yoka anso yatshisanu
ndi tshitatu, ndimo iri ya isanu ndi iwiri; ndimo ipita kwa
12 kumwaza. Ndi nyanga kumi zomwe unaona ziri mafumu
otshuka kumi, omwe sanalandira palibe dziko monga kosu-
ntira; koma alandira kuweruza monga mafumu otshuka,
13 ndi nyama, kwa ora limodzi. Amene ali ndi muwongo
umodzi, ndimo apatsa kuweruza kwao ndi mpamvu kwa
14 nyama. Amene adzapanga nkondo pa Mwana wa nkosa,
ndi Mwana wa nkosa adzapambana awo, kuti ali Mwini wa
eni, ndi Fumu Yotshuka ya mafumu otshuka; ndimo awo
*onso adzapambana* omwe ali nai', akuitanidwa ndi osang'-
15 kidwa ndi amvanu. Ndimo anena ndi ine, Madzi omwe
unaona, pomwe nkazi wa dama akala, ali antu, ndi antu
16 ambiri, ndi mitundu, ndi maliu. Ndi nyanga kumi zomwe
unaona, ndi nyama, zimene zidzakwiira nkazi wa dama,
ndimo zidzapanga ie wadzinja ndi womariseke, ndimo zidza-
17 dia nyama yatshi, ndimo zidzaotsha ie konse ndi moto. Kuti
Mulungu naika m' mitima yao ku tshita muwongo watshi,
ndi ku fika kwa muwongo umodzi, ndi ku patsa dziko lao
18 kwa nyama, kwa ntawi mau a Mulungu akanatedwa.
Ndimo nkazi emwe unaona ali mzinda woukuru, womwe
uweruza pa mafumu otshuka a dziko.

18 Pambuiu zintu zimenezi dinaona njelo wina kutsika kwa
kumwamba, kuli ndi kuweruza kwakukuru; ndimo dziko
2 linaunikidwa ndi kupambana kwatshi. Ndimo napfula ndi
liu lalikuru, kunena, Unagwa, unagwa Babilon woukuru,

ndimo unakala malo a ademon, ndi nyumba ya ndima ya
mizimu yosatsuka yonse, ndi nyumba ya ndima ya mbalame
zosatsuka ndi zokwiidwa zonse. Kuti ndi vinyo wa ku- 3
kwiira kwa dama latshi mitundu yonse inagwa; ndimo
mafumu otshuka a dziko natshita dama ndi ie, ndi amaronda
a dziko nalemeretswa ndi mpamvu ya kutshuruka kwatshi.
Ndimo dinamva liu lina kwa kumwamba, kunena, 4
Turukani, antu anga, mwa iwo, kuti musakala ndi unzatshi
ndi zimpulupulu zatshi, ndi kuti musalandira ndi dzaola
dzatshi: kuti mpulupulu zatshi zinafika inde kwa ku- 5
mwamba, ndi Mulungu wakumbukila mpulupulu zatshi.
Bwezani kwa iwo inde monga unabweza, ndimo pindulani 6
kawiri *kwa iwo* kupindula kawiri kofana ndi ntshito zatshi:
m' tshiko tshomwe unasang'kaniza, sang'kanizani kwa iwo
kawiri. M' bwanje kwambiri nadzipambanitsa, ndi unakala 7
woutshuruka, tshointsho kwambiri patsani iwo wa kuzunza
ndi wa kulira: kuti unena mu ntima watshi, Dikala
fumuyeikazi yotshuka, ndimo sindiri wamasie, ndimo
sindidzaona konse maliro. Ndimo m' siku limodzi dzaola 8
dzatshi dzidzafika, imfa, ndi maliro, ndi njala; ndimo iwo
udzaotshedwa konse ndi moto; kuti wolimba ali Mwini Mu-
lungu emwe naweruza iwo. Ndimo mafumu otshuka a dziko, 9
omwe anatshita dama nakala ndi moyo kotshuruka ndi iwo,
adzalira misozi ndimo adzapfula pa iwo, ntawi ayang'ana pa
utsi wa kupsa kwatshi, kuima kutali kwa kuopa kwa kuzunza 10
kwatshi, kuti, Tshaipa, tshaipa, mzinda woukuru, Babilon,
mzinda wolimba! kuti m' ora limodzi kuweruza kwako
kunafika. Ndimo amaronda a dziko alira misozi nalira pa 11
iwo, kuti palibe muntu agula maronda ao ntawi ina; maronda 12
a golide, ndi silivere, ndi miala yolemera, ndi maperile, ndi
nsaru zabwino za lini, ndi zakuda, ndi silike, ndi zofira; ndi
mtengo wonse wa taine, ndi dziwira dzonse dza nyanga wa njo-
bvu, ndi dziwira dzonse dzipangidwa dza mtengo wolemera
wopambana, ndi dza nkua, ndi dza tshitsulo, ndi dza marmore;
ndi sinamon, ndi zonung'kira, ndi zofukiza, ndi mafuta, ndi 13
nardo, ndi vinyo, ndi mafuta, ndi ufa wabwino, ndi trigu, ndi
zing'ombe, ndi zinkosa; ndi *maronda* a akavalo ndi matshariote
ndi akapolo; ndi mizimu ya antu. Ndi dzobala dzomwe nzimu 14
wako unafunira dzinatshoka kwa iwe, ndi zintu zonse zomwe
zinali zabwino ndi zambiri zinamwazika kwa iwe, ndi *antu*
sadzapeza izo palibe ntawi ina. Amaronda a zintu zimenezi, 15
omwe analemerezedwa ndi iwo, adzaima kutali kwa kuopa

16 kwa kuzunza kwatshi, kulira misozi ndi maliro; kuti,
Tshaipa, tshaipa, mzinda woukuru, iwo womwe unabvekedwa
ndi nsaru zabwino za lini ndi zakuda ndi zofira, ndimo
unabvekedwa ndi golide ndi miala yolemera ndi maperile!
17 kuti m' ora limodzi zolemere zazikuru zotere zipangidwa
zadzinja. Ndi ambuiye a dzombo onse, ndi onse omwe
aenda ndi matanga ku malo ena, ndi amarinyero, ndi monga
ambiri monga alandira moyo wao ndi nyanja, naima kutali,
18 napfula monga nayang'ana pa utsi wa kuotsha kwatshi, kuti,
19 *Mzinda* uti uli wofana mzinda woukuru? Ndimo naponya
fumbi pa mitu yao, napfula, kulira misozi ndi maliro, kuti,
Tshaipa, tshaipa, mzinda woukuru, momwe analemerezedwa
onse omwe anapotshera dzombo dzao m' nyanja ndi tshifukwa
tsha kutshuruka kwatshi! Kuti m' ora limodzi upangi-
20 dwa wadzinja. Sekerani pa iwo, mwamba iwe, ndi oyera
inu, ndi apostile inu, ndi aprofeti inu; kuti Mulungu
waweruza kuweruza kwanu pa iwo.
21 Ndimo njelo wolimba natukula mwala monga unali mpero
yeikuru, nauponya m' nyanja, kuti, Tshointsho ndi kugwa
kwakukuru Babilon, mzinda woukuru, udzagwetsedwa,
22 ndimo usadzapezedwa konse ntawi ina. Ndi liu la aharpe
ndi adziteta ndi akuomba milumbwi ndi alipenga silidza-
mvedwa konse mwa iwe ntawi ina; ndi waluso palibe, wa
luso lina, adzapezedwa konse mwa iwe palibe ntawi ina;
ndi liu la mpero silidzamvedwa konse mwa iwe palibe ntawi
23 ina; ndi kuunika kwa muni kusadzawala konse mwa iwe
palibe ntawi ina; ndi liu la wokwati ndi la tshikwati
silidzamvedwa konse mwa iwe palibe ntawi ina: kuti
amaronda ako anali otshuka a dziko; kuti ndi umabisalira
24 wako mitundu yonse inanyengedwa. Ndimo mwa iwo
unapezedwa mwazi wa aprofeti ndi wa oyera, ndi wa onse
omwe anapedwa pa dziko.

19 Pambuiu zintu zimenezi dinamva monga linali liu lalikuru
la antu ambiri m' mwamba, kunena, Haleluya; Kupulumu-
tsa, ndi kupambana, ndi mpamvu, ziri za Mulungu watu:
2 kuti oona ndi odeka ali maweruzo atshi; kuti waweruza
nkazi wa dama wang'kuru, emwe ananyansa dziko ndi dama
latshi, ndimo wazimbula mwazi wa akapolo atshi pa dzanja
3 latshi. Ndimo ntawi yatshiwiri anena, Haleluya. Ndimo
4 utsi watshi ukwera kwa magonero a magonero. Ndimo
akuru makumi awiri ndi anai ndi zamoyo zinai zinagwa
ndimo zinapembedza Mulungu emwe akala pa mpando

wotshuka, kunena, Amen; Haleluya. Ndi liu linaturuka 5
kwa mpando wotshuka, kunena, Patsani kulemekeza kwa
Mulungu watu, inu nonse akapolo atshi, inu nomwe muopa
ie, ang'ono ndi akuru. Ndimo dinamva monga linali liu la 6
antu ambiri, ndi monga liu la madzi ambiri, ndi monga liu la
mabingu akuru, kuti, Haleluya: kuti Mwini Mulungu watu,
Wampamvuyonse, aweruza. Tikondwere ndi tisekere kwa- 7
mbiri, ndi tipatse kupambana kwa ie: kuti kukwatitsa kwa
Mwana wa nkosa kwafika, ndi nkazi watshi wadzikonzetsa.
Ndimo kunapatsidwa kwa ie kuti akadzibvala m' nsaru yabwi- 8
no ya lini, yowala *ndi* yoyeretsa: kuti nsaru yabwino ya lini
iri ntshito zodeka za oyera. Ndimo anena ndi ine, Lemba, 9
Odala ali omwe aitanidwa ku ngonero wa kukwatitsa wa
Mwana wa nkosa. Ndimo anena ndi ine, Amene ali mau
oona a Mulungu. Ndimo dinagwa patsogolo pa mapazi 10
atshi ku pembedza ie. Ndimo anena ndi ine, Ona kuti
usakutshita: diri kapolo nzako ndi iwe ndimo ndi abali ako
omwe apotshera kumariza kwa Yesu: pembedza Mulungu:
kuti kumariza kwa Yesu kuli nzimu wa kulosa.

Ndimo dinaona mwamba motsegulidwa; ndi ona, kavalo 11
woyera, ndimo iemwe nakala pa ie, atshedwa Wamvanu ndi
Woona; ndimo m' kudeka aweruza ndi apanga nkondo.
Ndimo maso atshi *ali* lilume la moto, ndi pa mutu watshi 12
*ali* madiadema ambiri; ndimo apotshera dzina lolembedwa,
lomwe palibe modzi adziwa koma ie eka. Ndimo abveke*dwa* 13
m' mwinjiro wowazidwa ndi mwazi: ndimo dzina latshi
litshedwa Mau a Mulungu. Ndimo magulu a ankhondo 14
omwe ali m' mwamba anamtsata pa akavalo oyera, abveke-
dwa ndi nsaru yabwino ya lini, yoyera *ndi* yoyeretsa.
Ndimo mwa nkamwa mwatshi mpeni wa nkondo wokutwa 15
uturuka, kuti ndi iwo akamenya mitundu: ndimo adzawe-
ruza iwo ndi ntole ya tshitsulo: ndimo aponda tshiwira tsha
vinyo tsha vinyo wa nkarwe ya kukwiira kwa Mulungu
Wampamvuyonse. Ndimo apotshera pa mwinjiro watshi 16
ndi pa ntshafu yatshi dzina lolembedwa, FUMU YOTSHUKA
YA MAFUMU OTSHUKA, NDI MWINI WA ENI.

Ndimo dinaona njelo kuima m' dzua; ndimo napfula ndi 17
liu lalikuru, kuti ku mbalame zonse zomwe ziuluka pakati
pa mwamba, Idzani *ndi* musang'kanitsidwa kwa ngonero
woukuru wa Mulungu; kuti mungodia nyama ya mafumu 18
otshuka, ndi nyama ya akazembe, ndi nyama ya antu
olimba, ndi nyama ya akavalo ndi ya omwe akala pa awo,

ndi nyama ya antu onse, aufulu ndi akapolo, ndi ang'ono
ndi akuru.
19 Ndimo dinaona nyama, ndi mafumu otshuka a dziko, ndi
magulu a ankhondo ao, anasong'kanidwa ku panga nkondo
pa ie emwe nakala pa kavalo, ndi pa gulu la ankhondo
20 latshi. Ndimo nyama inagwidwa, ndimo ndi ie mprofeti
wonyenga emwe anatshita zizindikilo m' kuona kwatshi, ndi
zomwe ananyenga awo omwe analandira lemba la nyama,
ndi omwe anapembedza fanizo latshi: awa awiri anaponye-
dwa amoyo, m' nyanja ya moto yomwe ipsa ndi sulfure:
21 ndimo otsala anapedwa ndi mpeni wa nkondo wa ie emwe
nakala pa kavalo, *inde mpeni wa nkondo* womwe unaturuka
m' nkamwa mwatshi: ndi mbalame zonse zinakuta ndi
nyama zao.

20 Ndimo dinaona njelo kutsika kwa kumwamba, kupotshera
fungulo ya phompo ndi unyolo woukuru m' dzanja latshi.
2 Ndimo nagwira nsatu, njoka yakali, yomwe iri Diabolos ndi
3 Satana, namanga ie kwa dzaka zousan, naponya ie m'
phompo, na*li*tseka, na*li*sindikiza pa ie, kuti sakanyenga
anso mitundu, kwa ntawi dzaka zousan dzikatedwa: pambuiu
dzimene akanamasulidwa kwa ntawi yeing'ono.
4 Ndimo dinaona mipando yotshuka, ndi anakala pa iyo,
ndimo kuweruza kunapatsidwa kwa awo: ndimo *dinaona*
mizimu ya awo omwe anadulidwa mutu kwa kumariza kwa
Yesu, ndi kwa mau a Mulungu, ndi otere omwe sanapembe-
dza nyama, kapena fanizo latshi, ndimo sanalandira lemba
pa pumi yao ndi pa dzanja lao; ndimo nakala ndi moyo,
5 naweruza ndi Kristu dzaka zousan. Otsala a akufa sanakala
ndi moyo kwa dzaka zousan dzikatedwa. Kumene kuli
6 kuukirira koiamba. Wodala ndi woyera ali ie emwe ali ndi
pande m' kuukirira koiamba: pamwamba pa awo imfa
yatshiwiri iribe mpamvu; koma adzakala adzukuru a
Mulungu ndi a Kristu, ndimo adzaweruza ndi ie dzaka
zousan.
7 Ndimo ntawi dzaka zousan dzitedwa, Satana adzamasu-
8 lidwa kwa nyumba ya ndima yatshi, ndimo adzaturuka ku
nyenga mitundu yomwe iri m' ngondia zinai za dziko, Goge
ndi Magoge, ku song'kanitsa iyo kwa nkondo: kuwerenga
9 kwa yomwe kuli monga ntshenga wa nyanja. Ndimo
inakwera pa kupingasa kwa dziko, ndimo inazungulira
masasa a oyera, ndi mzinda wokondedwa: ndi moto unatsika
10 mwa kumwamba, ndimo unadia iyo. Ndimo diabolos emwe

ananyenga iyo anaponyedwa m' nyanja ya moto ndi sulfure,
momwe ziri inso nyama ndi mprofeti wonyenga; ndimo
adzazunzidwa msana ndi usiku kwa magonero a magonero.

Ndimo dinaona mpando wotshuka woukuru woyera, ndi 11
ie emwe nakala pa iwo, kwa nkope ya emwe dziko ndi
kumwamba zinatawa; ndimo anapezedwa palibe malo kwa
izo. Ndimo dinaona akufa, akuru ndi ang'ono, kuima 12
patsogolo pa mpando wotshuka; ndi mabuku anatsegulidwa:
ndimo buku lina linatsegulidwa, lomwe liri *buku* la moyo:
ndimo akufa anaweruzidwa mwa zintu zomwe zinalembedwa
m' mabuku, kwa ntshito zao. Ndimo nyanja inapereka 13
akufa omwe anali mwa iyo; ndimo imfa ndi Hadesi zina-
pereka akufa omwe anali mwa izo: ndimo anaweruzidwa
antu onse kwa ntshito zao. Ndimo imfa ndi Hadesi 14
zinaponyedwa m' nyanja ya moto. Imene iri imfa yatshi-
wiri, *inde* nyanja ya moto. Ndimo ngati wina sanapezedwa 15
wolembedwa m' buku la moyo, anaponyedwa m' nyanja
ya moto.

Ndimo dinaona mwamba mwatsopano ndi dziko latso- 21
pano: kuti mwamba moiamba ndi dziko loiamba zinapita;
ndimo nyanja iribe enso. Ndimo dinaona mzinda woyera, 2
Yerusalem watsopano, kutsika kwa kumwamba kwa
Mulungu, ufotokozedwa monga tshikwati wokonzetsedwa
kwa mamuna watshi. Ndimo dinamva liu lalikuru kwa 3
mpando wotshuka kuti, Ona, msasa wa Mulungu uli ndi
antu, ndimo adzakala ndi awo, ndimo adzakala antu atshi,
ndi Mulungu eka adzakala ndi awo, *ndimo adzakala* Mulu-
ngu wao: ndimo adzapukuta misozi yonse kwa maso ao; 4
ndimo imfa idzakala palibe ntawi ina; kapena sizidzakala
maliro, kapena kulira, kapena ululu, palibe ntawi ina:
zintu zoiamba zinapita. Ndimo ie emwe akala pa mpando 5
wotshuka nati, Ona, dipanga zintu zonse zatsopano. Ndimo
ati, Lemba: kuti mau amene ali amvanu ndi oona. Ndimo 6
nanena ndi ine, Anakala. Diri Alefa ndi Omega, kuamba
ndi kuta. Didzapatsa kwa ie emwe amva ludzu ndi
kasope wa madzi a moyo kolere. Iemwe apambana adza- 7
loa zintu zimenezi; ndimo didzakala Mulungu watshi,
ndimo adzakala mwana wanga. Koma kwa akuopa, ndi 8
akusamvana, ndi onyansa, ndi ambanda, ndi adama, ndi
oombedza ula, ndi opembedza mafano, ndi amabodza onse,
pande lao *lidzakala* m' nyanja yomwe ipsa ndi moto ndi
sulfure; yomwe iri imfa yatshiwiri.

9 Ndimo nadza modzi wa anjelo asanu ndi awiri omwe
anali ndi zimbizi zisanu ndi ziwiri, omwe anapatikizidwa
ndi dzaola dzisanu ndi dziwiri dzakutungo; ndimo nala-
nkula ndi ine, kuti, Idza kuno, didzasonyeza iwe tshikwati,
10 nkazi wa Mwana wa nkosa. Ndimo nanyamula ine m'
Nzimu kwa piri lalikuru ndi lalitali, nasonyeza ine mzinda
woyera Yerusalem, kutsika mwa kumwamba kwa Mulungu,
11 kupotshera kupambana kwa Mulungu: muni watshi unali
wofana ndi mwala wa ntengo wapatali, monga unali mwala
12 wa yaspis, waonekera monga kristalo: kuli ndi koma
lalikuru ndi lalitali; kuli ndi dzipata kumi ndi dziwiri,
ndi pa dzipata anjelo kumi ndi awiri; ndi maina alembedwa
pa idzo, omwe ali *maina* a mafuko kumi ndi awiri a ana a
13 Sirayeli: pa bvuma dzinali dzipata dzitatu; ndi pa mpoto
dzipata dzitatu; ndi pa mwela dzipata dzitatu; ndi pa
14 zambwe dzipata dzitatu. Ndimo koma la mzinda linali ndi
maziko kumi ndi awiri, ndi pa awo maina kumi ndi awiri
15 a apostile kumi ndi awiri a Mwana wa nkosa. Ndimo
iemwe analankula ndi ine anapotshera kwa muyezo nzengo
yagolide ku linganiza mzinda, ndi dzipata dza iwo, ndi
16 koma la iwo. Ndimo mzinda uli kulinganira kanai,
ndi mulitali mwa iwo muli mwamukuru monga ndi
mkupingasa: ndimo nalinganiza mzinda ndi nzengo, masta-
dia mazousan kumi ndi awiri: mulitali ndi mkupingasa ndi
17 mkuzuka za iwo ziri modzimodzi. Ndimo nalinganiza
koma la iwo, mikono makumi okaoka kumi, ndi makumi
anai ndi inai, *monga ndi* muyezo wa muntu, womwe uli wa
18 njelo. Ndimo kumanga kwa koma la iwo kunali kwa
yaspis: ndi mzinda unali golide losasang'kaniza, lofana
19 ndi glase loyera. Maziko a koma la mzinda anakonzetsedwa
ndi mitundu yonse ya miala yolemera. Kuzika kwatshi-
modzi kunali yaspis; kwatshiwiri, safiro; kwatshitatu,
20 kalkedon; kwatshinai, smarado; kwatshisanu, sardonis;
kwatshisanu ndi tshimodzi, sardiyo; kwatshisanu ndi tshi-
wiri, krizolito; kwatshisanu ndi tshitatu, berilo; kwatshi-
sanu ndi tshinai, topaziyo; kwakumi, krizopazo; kwakumi
ndi tshimodzi kakinto; kwakumi ndi tshiwiri, hametisto.
21 Ndimo dzipata kumi ndi dziwiri dzinali maperile kumi ndi
awiri; dzonse dzipata dzinali tshimodzi ndi tshimodzi perile
limodzi: ndi kwalala la mzinda linali golide losasang'kaniza,
22 monga linali glase lakuonikera. Ndimo sindinaona tempile
umo: kuti Mwini Mulungu Wampamvuyonse, ndi Mwana

wa nkosa, ali tempile la iwo. Ndimo mzinda wosali ndi 23
kufunidwa ndi dzua, kapena mwezi, ku wala pa iwo: kuti
kupambana kwa Mulungu kunaunika iwo, ndi muni wa iwo
*uli* Mwana wa nkosa. Ndimo mitundu idzaenda pakati pa 24
kuunika pa iwo: ndimo mafumu otshuka a dziko atenga
kupambana kwao mwa iwo. Ndimo dzipata dza iwo 25
sidzidzatsekedwa konse msana (kuti sikudzakala usiku apo):
ndimo adzatenga kupambana ndi ulemu za mitundu 26
mwa iwo: ndimo sikudzaloa konse kantu kena kanko, 27
kapena iemwe atshita tshonyansa ndi bodza: koma awo
oka omwe alembedwa m' buka la moyo la Mwana wa nkosa.
Ndimo nasonyeza ine ntsinje wa madzi a moyo, woye- 22
zimira monga kristalo, kuturuka kwa mpando wotshuka
wa Mulungu ndi wa Mwana wa nkosa, pakati pa kwalala la 2
iwo. Ndimo patsidia lino la ntsinje ndi patsidia lidya unali
ntengo wa moyo, kubala *mitundu* kumi ndi iwiri *ya* dzobala,
kubala dzobala dzatshi miezi yonse: ndi masamba a ntengo
anali kwa kutshiritsa kwa mitundu. Ndimo kudzali palibe 3
tukwano onso: ndi mpando wotshuka wa Mulungu ndi wa
Mwana wa nkosa udzakala momo: ndi akapolo atshi
adzaimirira ie; ndimo adzaona nkope yatshi; ndi dzina 4
latshi *lidzakala* pa pumi zao. Ndimo kudzali usiku palibe 5
ntawi ina; ndimo osafuna palibe kuunika kwa muni,
kapena palibe kuunika kwa dzua; kuti Mwini Mulungu
adzapatsa awo kuunika: ndimo adzaweruza kwa magonero
a magonero.

Ndimo ananena ndi ine, Mau amene ali amvanu ndi oona: 6
ndi Mwini, Mulungu wa mizimu ya aprofeti, natumiza njelo
watshi ku sonya kwa akapolo atshi zintu zomwe zikanafika
nsanga. Ndimo ona, difika nsanga. Wodala ali ie emwe 7
adondoloza mau a kulosa kwa buku limene.

Ndimo ine Yohane diri ie emwe dinamva ndinaona zintu 8
zimenezi. Ndimo ntawi dinamva ndinaona, dinagwa ku
pembedza patsogolo pa mapazi a njelo emwe anasonya ine
zintu zimenezi. Ndimo anena ndi ine, Ona kuti usaku- 9
tshita: diri kapolo nzako ndi iwe ndimo ndi abali ako
aprofeti, ndimo ndi awo omwe adondoloza mau a buku
limene: pembedza Mulungu.

Ndimo anena ndi ine, Usasindikiza mau a kulosa kwa 10
buku limene; kuti ntawi iri pafupi. Iemwe ali wosadeka, 11
atshite kusadeka koyenjezayenjeza: ndimo iemwe ali wo-
nyansa, apangidwe wonyansa koyenjezayenjeza: ndimo

iemwe ali wodeka, atshite kudeka koyenjezayenjeza:
ndimo iemwe ali woyera, ayeretsedwe koyenjezayenjeza.
12 Ona, difika nsanga; ndi sekeretso langa liri ndi ine, ku
13 bweza ku antu onse ndi monga ntshito zao ziri. Diri Alefa
ndi Omega, watshimodzi ndi wakutungo, kuamba ndi
14 kuta. Odala ali awo omwe atsuka miinjiro yao, kuti
angopotshera mpamvu *ku fika* kwa ntengo wa moyo, ndimo
15 angoloa mwa dzipata munzinda. Kunja ali agaru, ndi
oombeza ula, ndi adama, ndi ambanda, ndi opembedza
mafano, ndi onse omwe akonda ndimo apanga bodza.

16 Ine Yesu datumiza njelo wanga ku mariza kwa inu zintu
zimenezi pa maeklesia. Diri ntsitsi ndi fuko za Davide,
nyenyezi ya mawa, yawala.

17 Ndimo Nzimu ndi tshikwati anena, Idza. Ndi iemwe
amva, anene, Idza. Ndi iemwe amva ludzu, afike: iemwe
afuna, atenge madzi a moyo kolere.

18 Dimariza kwa antu onse omwe amva mau a kulosa kwa
buku limene, ngati muntu modzi adzaong'khetsa kwa awo,
Mulungu adzaong'khetsa kwa ie dzaola dzomwe dzilembedwa
19 m' buku limene: ndimo ngati muntu modzi adzatshotsa
kwa mau a buku la kulosa kumene, Mulungu adzatshotsa
pande latshi kwa ntengo wa moyo, ndi kwa mzinda woyera,
zomwe zilembedwa m' buku limene.

20 Iemwe amariza zintu zimenezi anena, Inde: difika
nsanga. Amen: idza, Mwini Yesu.

21 Kufatsa kwa Mwini Yesu kukale ndi oyera. Amen.